

MFUNDO ZONADI ZENIZENI ZA BUKHU LOPATULIKA

Maphunziro Owerenga

Kuwulura Za Chimwemwe Ndi
Mtendere Mu Chikristu Choona

Duncan Heaster

**MFUNDO ZONADI
ZENIZENI ZA BUKHU
LOPATULIKA**

DUNCAN HEASTER

Bible Basics

English Edition first published 1992

Chichewa Edition published 2005, reprinted 2011

Bible Basics is also available in:

Afrikaans, Albanian, Amharic, Arabic, Armenian, Chinese, Estonian, Farsi, French, Georgian, Hebrew, Hungarian, Hindi, Igbo, Italian, Japanese, Kazakh, Korean, Latvian, Lithuanian, Macedonian, Mongolian, North Sotho, Polish, Portuguese, Russian, Serbo-Coat, Slovak, Spanish, Tagalog, Telugu, Turkish, Ukrainian

To view available translations on-line see
<http://www.biblebasicsonline.com>

<http://www.carelinks.net>

Published by
Christadelphian Advancement Trust
Company No. 3927037 Reg. Charity No. 1014615
PO Box 3034
South Croydon, Surrey CR2 0ZA
ENGLAND

Carelinks Publishing, PO Box 152, Menai NSW 2234 AUSTRALIA

© Duncan Heaster – 2005

PHUNZIRO 1: MULUNGU	1
1.1. Mulungu Alipo	
1.2 Mawonekedwe A Mulungu	
1.3 Dzina La Mulungu Ndi Makhalidwe Ake	
1.4 Angelo	
PHUNZIRO 2: MZIMU WA MULUNGU	39
2.1 Mzimu Wa Mulungu – Tanthawuzo	
2.2 Mauziridwe (Mapatsidwe A Mau Ndi Mulungu)	
2.3 Mphatso Za Mzimu Woyera	
2.4 Kuchotsedwa Kwa Mphatso	
2.5 Baibulo Lamulo Lokhalo	
PHUNZIRO 3 : MALONJEZANO A MULUNGU	115
3.1 Malonjezano A Mulungu Oyamba	
3.2 Malonjezano A M’unda Wa Edeni	
3.3 Malonjezano Kwa Nowa	
3.4 Malonjezano Kwa Abrahamu	
3.5 Malonjezano Kwa Davide	
PHUNZIRO 4 : MULUNGU NDI IMFA	160
4.1 Uthunthu Wa Munthu	
4.2 Thunthu - (Mzimu)	
4.3 Mzimu Wa (Mphamvu Ya) Munthu	
4.4 Kipa Imfa Ndiko Kusapuma Komanso Kusakumbukira	
4.5 Kuukanso Kwa Akufa	

- 4.6 Chiweruzo
- 4.7 Malo Olandirira Mphotho: Kumwamba Kapena Pansi?
- 4.8 Udindo Wathu Pamaso Pa Mulungu Yehova
- 4.9 Helo (Manda Kapena Kuti Dzenje)

PHUNZIRO 5 : UFUMU WA MULUNGU 216

- 5.1 Kufotokozero Za Ufumu Wa Mulungu
- 5.2 Ufumu Wa Mulungu Sunakhazikitsidwe
- 5.3 Ufumu Wa Mulungu Kalelo
- 5.4 Ufumu Wa Mulungu Mtsogolomo
- 5.5 Chirumika

PHUNZIRO 6 : MULUNGU KOMANSO CHAKWAYIPA 254

- 6.1 Mulungu Komanso Chakwayipa
- 6.2 Mdierekezi Ndi Satana
- 6.3 Daimoni (Mizimu Yonyansa)

PHUNZIRO 7 : CHIYAMBI CHA YESU 316

- 7.1 Uneneri Wa Yesu M'chipangano Chatsopano
- 7.2 Kubadwa Mwa Namwali
- 7.3 Udindo Wa Khristu Mchikonzero Cha Mulungu
- 7.4 "Pachiyambi Panali Mau" Yohane 1:1-3

PHUNZIRO 8 : UTHUNTHU WA YESU 352

- 8.1 Uthunthu Wa Yesu – Mwachidziwitso

- 8.2 Kusi yana Pakati Pa Mulungu Ndi Yesu Khristu**
- 8.3 Uthunthu Wa Yesu**
- 8.4 Umunthu Wa Yesu**
- 8.5 Ubale Umene Ulipo Pakati Pa Mulungu Ndi Yesu**

PHUNZIRO 9 : NTCHITO YA YESU 371

- 9.1 Chigonjetso Cha Yesu**
- 9.2 Mwazi Wa Yesu**
- 9.3 Nsembe Ya Ife Ndi Iye Yekha**
- 9.4 Yesu Ndiye Amatiyimira Kwa Mulungu**
- 9.5 Yesu Potsagana Ndi Lamulo La Mose**
- 9.6 Sabata**

PHUNZIRO 10 : KUBATIZIDWA MWA YESU 403

- 10.1 Kufunika Kwa Kukulu Kwa Ubatizo**
- 10.2 Kodi Tingabatizidwe Bwanji**
- 10.3 Tanthauzo La Ubatizo**
- 10.4 Ubatizo Ndi Chipulumutso**

PHUNZIRO 11 : UMOYO MWA YESU 434

- 11.1 Chiyambi**
- 11.2 Kudziyeretsa/ Kudzipatula**
- 11.3 Ntchito Yoyenera Kuchita Mu Chikhristu Chathu**
- 11.4 Ukwati**
- 11.5 Kusonkhana Mogwirizana**

PHUNZIRO 1
MZIMU WA MULUNGU

1.1.MULUNGU ALIPO

“...Pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndikuti ali wobwezera mphoto iwo akumfuna Iye” (A Hebr 11:6) Cholinga cha phunziro lino ndicho; kuthandiza onse omwe akufunitsitsa kusendera pafupi ndi Mulungu popeza iwo akudziwa kuti **“Mulungu Alipo”** choncho, sitifuna kutaya nthawi yawo powawuza kuti Mulungu alipo popeza iwowa akudziwa kale. Chimene tidzachita pano ndiye kuwonetsetsa ndi kufufuza zambiri mofananiza momwe matupi athu akuwonekera (Masalmo 139:14), tiwonanso ndi chidwi m'mene duwa limawonekera pa chilengedwe chake, kukula kwa mlenga lenga (m'malere), zonsezi zikuwonetse kwaife kuzizwitsa ndi mawonekedwe ake kuti ndizoonadi, sizinalengedwe zokha ayi. Kotero, kuti munthu wina lero anene kuti kudziko kuno kulibe Mulungu, ndizofunika chikhulupiriro chozama chomwe chiyenera kuposa chikhulupiriro tiri nacho lerochi pa Yesu; chikhulupiriro chatu kawiri kawiri chikuwonetseratu kuti Mulungu alipo ndipo kupeza chikhulupiriro ichi, ndi kobvuta kwambiri. Tangoganizirani nokha kuti kusakhale Mulungu, sipangakhale tanthawuzo leni leni lomwe analengera dziko lino ndi zonse ziri m'menemo; palibe tanthawuzo kuti kukhale usiku, masana ndi zina zotero. Chifukwa chaichi, ndizosadabwitsa kuwona kuti pafupifupi aliyense padziko lapansi amadziwa ndipo amakhulupirira kuti Mulungu alipo komanso kuti Mulunguyo amagwira ntchito yaikulu pakati paife kudzera mu zomwe zimawoneka padziko.

Tikudziwanso kuti ngakhale tonse tingabvomerezane kuti kudziko kuno kuli Mulungu, timasiyana mu kazindikiridwe monga kuti Mulungu'yo lero Mphamvu zake ziri bwanji pakati pathu, nanga malonjezano ake kwaife ndi chiyani, atanthawuzanji maka tikakhulupirira ndi kuchita chifuniro chake? Nanga ine ngati m'modzi olengedwa ndi Iye ndingakwaniritse bwanji cholinga chake paine (yense payekha payekha)? Paulo mkalata yake kwa a Hebr 11:6 akuti;

“....ayenera kukhulupirira kuti (Mulungu) alipo

NDINSO

“...kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye”.

Nkhani yaikulu mu Baibulo inkakhudza ana ake a ku Israeli ndipo nthawi zonse, Mulungu ankawadzudzula kuti zochita zawo ndi mabvomeredwe awo sakugwirizana ndi chikhulupiriro chawo mu malonjezano a Mulungu. Mose anawauza ana a Israeli; **“...dziwani lerolino nimukumbukire m’mitima mwanu, kuti Yehova ndiye Mulungu m’thambo la Kumwamba ndi dziko lapansi; Palibe wina. Muzisunga malembo ake ndi malamulo ake”** (Deuteronomo 4:39,40).

Munjira iyi tiyenera kuzindikira kuti ngakhale tidziwe kuti Mulungu alipo koma osachitapo kanthu, tiri chabe. Mulungu Mwini amafuna ife “tichitepo kanthu” **“...muzisunga malembo ake ndi malamulo ake...kuti masiku anu achuluke.”** Choncho, cholinga cha maphunziro ano mu buku lino, ndi kufuna kuphunzitsana zambiri za malamulo amene’wa ndi m’mene tingawasungire. Tikasanthula malembo Oyera, mu maphunziro awa, tiwonanso kuti chikhulupiriro chathu chidzakula ndikuzindikira zambiri za kukhala ndi Mulungu.

“...Chikhulupiriro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa Mau a Mulungu” (Aroma 10:17). Tikawerenganso Yesaya 43:9-12, tiwona kuti kuzindikira uneneri ndi malosero a Mulungu kudzera mwa a losi ndi aneneri ake, akutiuzza kuti dzina lake lenileni la Mulungu ndi **“ Chiyambire nthawi, ‘Ine Ndine’ ”** (Yesaya 43:13). Izi zikuphera ndemanga dzina loti; **“INE NDINE YEMWE NDIRI INE”** pa ndime ya Eksodo 3:14. Mtumwi Paulo pofika ku Bereya komwe ndi ku mpoto kwa dziko la Greece, analalikira za **“Uthenga Wabwino”** wa Mulungu. M’malo moti anthu a chi Herene aja angokhulupirira zonse zomwe Paulo analalikira monga zikuchitikira ndi ife mu mipingo yathu lero, timva kuti anthu onse; **“...analandira Mau aja ndi kufunitsitsa (ndi luntha) ndi mtima onse; nasanthula m’malembo masiku onse, ngati zinthu zonse zinali zotero. Ndipo ambiri a iwo anakhulupirira...”** (Machitidwe 17:11-12). Apa tiwona kuti pali kusiyana kwakukulu pakati paife ndi anzathu awa a chi Helene. Iwo anaulandira **“Uthenga wa Mulungu”** (osati wa Paulo ayi), ndipo atapita ku nyumba zawo anakhala panso nasanthulanso Mau mu Buku Lopatulika pofananiza ndi zomwe Paulo analalika ndipo ataona kuti zinali zoonadi, anakhulupirira nazitsata pomutsimikizira Paulo kuti analalika zoonadi. Izi

zikusiyana koposa ndi zomwe zikuwoneka masiku ano m'matchalitchi athu komwe anthu amatembenuka mtima asanafufuze okha mu Buku Loyera ngati momwe anachitira anzathu ku Bereya pa nthawi ya Paulo. Kodi ife tiri nawo mtima wofuna kufufuza mu Baibulo tisanakhulupirire zonse zomwe zalalikidwa ndi kulembedwazi? Kufufuza koyenera ndikuzindikira bwino chomwe mwamva ndi gawo lomwe likusowa kwambiri pakati pathu. N'chifukwa chake tiyenera kumvetsetsa bwino kuti tipindulepo mu moyo wathu wachikhristu chatsopano. Izi zingathandize kuteteza Mau a Mulungu kuti anthu ena asatisokoneze.

Tikhulupirira kuti buku lino likukwaniritsa cholinga choti yense wainu aphunzire ndondomeko yoyenera pamene munthu wina aliyense akufuna kuphunzira mofufuza magawo onse a malembo Oyera. Mwaichi, mukazindikira, mudzakhulupirira ndi kuchita chifuniro chake pomvera motsata ndondomeko yake imeneyi. Pali kusiyana pakati pa kumva "Mau a Uthenga Wabwino" ndikukhala ndi chikhulupiriro mu Mau amenewa ndipo izi zawonetsedwa mu ndime zapatsidwa pansizi:

-“...*Ambiri kwa Akorinto atamva anakhulupirira nabatizidwa..*” (Machitidwe 18:8)

-“...*amve Mau a Uthenga Wabwino, nakhulupirire..*”(Machitidwe 15:7)

-“...*Kotero tilalikira, ndi kotero munakhulupirira*” (1 Akorinto 15:11)

-“...*Mbeu*” mu “*fanizo la ofesa*” ndiwo Mau a Mulungu (Luka 8:11) pamene “*Mbeu*” ya mu “*fanizo la kambeu ka mpiru*” ndiye chikhulupiriro (Luka 17:6) ndipo powona kuti “*Chikhulupiriro chidza pobvomereza Mau a ulaliki m'chikhulupiriro*” (Aroma 10:8-9); “*woleredwa m'mauwo achikhulupiriro ndi malangizo abwino.*” (1 Timoteo 4:6) kwaiwo omwe ali ndi mitima yotseguka kuti akakhulupirire mwa Mulungu m'mau ake (Agalatiya 2:2; A Hebri 4:2).

-Yohane polemba za umoyo wa Ambuye Wathu Yesu Khristu anati; “...*adziwa kuti anena zoonso mukakhulupirire*” (Yohane 19:35) kotero tinenetsa kuti Mau a Mulungu ndiye “*choonadi*” (Yohane 17:17) choncho, tiyenera

kuwakhulupirira. Zoonadi Mulungu adalipo kalelo, alipo lero ndipo adzakhalapo.

1.2 MAWONEKEDWE A MULUNGU

Mfundo iyi ndi imodzi yozizwitsa kwaife tikayamba kuganizira za maonekedwe a Mulungu chifukwa timamva kuti palibe yemwe anamuona Mulungu. Baibulo limatiuza kuti Mulungu amaoneka ngati momwe munthu amawonekera. Timadziwanso kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu kotero kuti ndi chifukwa chake Yesu'yo adaonekanso ngati momwe munthu amaonekera. Werengani a Heberi 1:3; (makamaka ma 'version' a Chingerezi). Munthu analengedwa mu chifanizo ndi m'chikhalidwe cha Mulungu (Genesis 1:26-27). Ndikhulupirira kuti kukadakhala kobvuta kuti kukhale Mulungu yemwe sankadziwika maonekedwe ndi makhalidwe ake, zingakhale zobvuta kwambiri kuti timukhulupirire Mulungu wotere opanda maonekedwe ndi uthunthu wake. Zikomo kuti maonekedwe ndi chikhalidwe cha Yesu zonse zidaonetsa chithunzi-thunzi cha Mulungu! Lero timadziwona komanso timadziwa kuti tiri mu maonekedwe a Mulungu, kungoti timasoweka chikhalidwe chake chomwe tiyenera kuchiphunzira mu Mau ake Oyera. Leronso ndikukhulupirira kuti chithunzi-thunzi choti Mulungu alibe maonekedwe chachoka mu mitima mwathu chifukwa taphunzira kuti Mulungu amaoneka ngati momwe ife tiri'li; tiri mu chifanizo chake cha Mulungu (chingerezi-image of God which is not equal in any way to the chichewa translation of "chizindikiro" but "chifanizo" that is "chofanana"). Mulungu sali ngati momwe akhristu ambiri amaganizira ayi koma ngati momwe Baibulo limanenera (in our own image). Ifeyo ndife ofanana mu maonekedwe ndi Namalenga Wathuyo. Ichi ndiye chiphunzitso ndi chikhulupiriro cha Baibulo.

Mulungu amasiyana ndi ife chifukwa iye ndi wamkulu ndipo titha kumuona Iye mu malonjezano ake. Chikhulupiriro cha ana a Israeli chinali choperewera kotero sanathe kuona maonekedwe eni eni a Mulungu (Yohane 5:37; Deuteronomo 4:12), ndipo izi zikuwonetseratu kuti Mulungu ayenera kukhala mu uthunthu Wake. Chikhulupiriro chotere chimakhalapo chifukwa chozindikira bwino-bwino mau ake a Chiuta ndinso chikhulupiriro m' mau ake'wo.

-“...*odala ali oyera mtima; chifukwa adzaona Mulungu*” (Mateyu 5:8)

-“...*ndipo akapolo ake adzamtumikira Iye, nadzaona nkhope yake, ndi dzina lake* (Dzina la Mulungu – Chibvumbulutso 3:12) *lidzalembedwa pamphamvu yake*” (Chibvumbulutso 22:3,4).

Chiyembekezo chamtundu wotere ndi chomwe chingabweretse kusintha kweni-kweni m'miyoyo yathu chifukwa chikutionetsa chithunzi-thunzi cheni-cheni cha nkhope ndi uthunthu wa Ambuye. Ambuye Mulungu wathu timakhala naye mu kazindikiridwe kathu za momwe Iye amaonekera kotero timadziwa kuti tikupembedza kwa Mulungu wooneka motere.

-“...*Londolani mtendere ndi anthu onse, ndi chiyeretso chimene, akapanda ichi, palibe m' modzi adzawona Ambuye,* (A Hebri 12:14).

Sitiyenera kulumbira chifukwa, “...*Yense wakulumbira kutchula kumwamba, alumbira chimpano cha Mulungu, ndi Iye wakhala pomwepo*” (Mateyu 23:22).

Zonse zomwe tikuwerengazi sizinalembedwa zikanakhala kuti Mulungu alibe maonekedwe kapena uthunthu wake weni weni.

“...*ndipo sichinaoneke chimene tidzakhala . Tidziwa kuti, pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, Pakuti tidzamuona Iye monga ali.* (1 Yohane 3:2,3) *...Ndipo wakukhala nacho chiyembekezo ichi pa Iye, adziyeretsa yekha, monga Iyeyu ali woyera.*”

Tikhoza kuona kuti sitidziwa zambiri zokhudza Mulungu Wathu komabe ngakhale ziri choncho, tikalalakala kumudziwa ndipo ngati tamudziwadi, tidzakumana naye m' masomphenya Mulungu Ambuye Wathu, ndikumuzindikira pochita zofuna zake. Kotero m' mabvuto ndi mazuzo oopsya, Yobu anasangalala chifukwa anali ndi ubale wokwanira ndi Mulungu wake popeza anamudziwa bwino lomwe. Chiyembekezo chake chinayima pa chizindikiro cha tsiku lomaliza lachiweruzo:

“...Ndipo khungu langa litaonongeka, Pamenepo ngakhale thupi langa, ndidzapenya Mulungu. Amene ndidzampenya ndekha, Ndi maso anga ndidzamuona siwina ayi.” (Yobu 19:26-27).

Mu mazuzo ngati omwewa, Paulo analiranso pofuula motere:

“...Pakuti tsopano tipenya mkalilole, ngati chimbuuzi; koma pomwepo maso ndi maso...” (1 Akorinto 13:12).

UMBONI WOPEZEKA MCHIPANGANO CHAKALE

Monga tawerenga mu Chipangano Chatsopano za maonekedwe a Mulungu kuti ndi ofanana ndi munthu, Chipangano Chakale sichikusiyanso ndi mfundo'yi. Baibulo iri ndi ndondomeko yokwanira kufotokoza bwino lomwe zambiri ya Mulungu, maonekedwe ake, komanso zomwe Mulunguyo amatha kuchita kotero ife sitingawiringule chifukwa zonse tiri nazo pakati pathu. Mwanjira iyi titha kudziwa komanso kudalitsika poona kuti ifeyo tiri m'chifaniziro chake cha Mlengi Wathu. Sitinalengedwe pachabe ayi, koma pamaziko ake a Chiuta ndi cholinga chomwe chiyenera kutilimbikitsa mu chikhulupiriro ndi chiyembekezo choonadi choyenera chomwensu chatsamira pa Mulungu Mwini, wofanana mu maonekedwe ndi ife. Kodi inu muli nawo maonekedwe amenewa? Ndime zotsatirazi zititsimikizira chizindikiro chimenechi:-

“...Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'chifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu...”(Genesis 1:26).

Choncho, munthu analengedwa mu chifanizo (mofanana) ndi makhalidwe a Umulungu; zizindikiro zomwensho zikupezeka mwa Angelo. Yakobo 3:9 akunena za “...*olengedwa m’chifanizo cha Mulungu*” (note:Chichewa translation here). Mau awerengedwa’wa sakukamba za mu mitima ndi maganizo athu ayi koma kaonekedwe mu thupi lathu; ndichifukwa chake maganizo athu ndi osiyana kwambiri ndi maganizo a Mulungu ngakhale kuti maonekedwe a uthunthu wathu ali ofanana ndi Mulunguyo. “...*Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutali ndi dziko lapansi, momwemonso njira zanga ziri zazitali kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu...*” (Yesaya 55:8,9). Kotero, maonekedwe ndi chifanifani chomwe chilipo pakati pa ife anthu ndi Mulungu ndicheni-cheni, palibe chisiyanitso chirichonse. Tikakumbuka za maonekedwe a Angelo pamene an’kawonekera kwa anthu, timamva kuti ankaoneka ngati anthu eni eni. Mwachitsanzo, Abrahamu anathandiza Angelo mosazindikira kuti anali Angelo. Iye ankayesa kuti anali anthu wamba chifukwa cha m’mene ankaonekera. Chilengedwe chathu mu chifanizo cha Mulungu ndichilimitso chachikulu kwa mkhristu aliyense popeza timakhala ndi chithunzi thunzi cheni cheni cha Mulungu yemwe timamupembedza. Izi zitanthauza kuti timapembedza Mulungu weni weni Yemwensho maonekedwe ake ali ngati ife anthu ake.

Angelo nawo, ndichinyezimiro ndi chifanifani cha Chiuta ngati momwe tiriri ife. Kotero, Mulungu anati kwa Mose, “*Ndidzanena naye pa Kamwa ndi pakamwa, moonekera...ndipo maonekedwe a Ambuye adzamufikira...*” (Numeri 12:8 again note that Chichewa translation is a problem here). Mau awa ndi omwe Mngelo wa Mulungu ananena kwa Mose kuti akuyimira dzina ndi maonekedwe a Yehova (werengani Eksodo 23:20,21). Apanso, tiwona kuti M’ngelo ndichifanifani mu maonekedwe ndi Mulungu choncho, tiwonanso kuti ngati M’ngelo adawoneka ngati munthu, koma munthu ndi chifani-fani ngakhaleenso mawonekedwe a Mulungu, ndiye kuti onse amafanana m’maonekedwe awo, komanso kuti munthu amafanananso ndi Mulungu Wake mu kaonekedwe. Choyenera kudziwa ndichakuti Mulungu ali pamwamba kwambiri mu machitidwe ake ngati Namalenga wa zonse mu mphamvu yake yoposa zolengedwa zonse. “...*Ambuye analankhula maso ndi maso ndi Mose, ngati momwe munthu alankhulira kwa bwenzi lake...*” (Eksodo 33:11; Deuteronomo

34:10). Apa tingati Mulungu anadza kwa Mose kudzera mwa m'ngelo yemwenso adawoneka ngati munthu nalankhula naye mu masomphenya.

-“*...Iye (Mlengi) amadziwa mapangidwe athu*” (Masalmo103:14); amafuna kuti ife tizindikire mawonekedwe onga a munthu mwa Iye, tate yemwe awonekansa ngati ana ake. N’chifukwa chake timawerenga mu Buku Lopatulika za maso, mikono, manja, mapazi a Mulungu ndi zina zotero. Izi ndi zomwe munthu ali nazonso ndipo zinalembedwa ndi cholinga chotsimikizira kuti munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu kotero, m’mene amawonekera munthu ndimomwenso amawonekera Mlengi Wake.

-Malo omwe Mulungu amakhalako tonse timadziwa kuti ndi kumwamba. Uku ndiye malo ake a Mulungu (Mlaliki 5:2). “*...Pakuti anapenya pansu ali Kumwamba kuli maso ake opatulika; Yehova pokhala Kumwamba anapenya dziko lapansi.*” (Masalmo 102:19,20); “*...Mverani Inu m’Mwamba mokhala Inu, ndi kukhulukira...*”(1 Mafumu 8:39). Komanso mwapadera, timawerenganso kuti Mulungu ali ndi “*Mpando Wa chifumu*” (2 Mbiri 9:8; Masalmo 11:4) Yesaya 6:1; Yesaya 66:1). Timayenera kumvetsa kuti kuzindikira malo eni eni omwe Mulungu amakhalako m’mwambamo ndi kobvuta popeza nzeru zathu ndi zoperewera koma titsimikizire kuti mphamvu zake, “*pa Mpando wa Chifumu Wake*” zilipodi ndipo kuti Iye mu Uthunthu Wake aliponso.

-Buku la Yesaya 45 limafotokoza kwambiri momwe Mulungu akukhudzidwira ndi zochitika mu chikhalidwe cha anthu padziko lino. “*Ine ndine Yehova ndipo palibe winanso...Ine ndine Yehova amene achita zonse izi...Ine Yehova ndinalenga zonsezi. Tsoka kwa iye amene akangana ndi Ine Mlengi Wake... Ine ndilenga mtendere ndi nkhondo ndi choyipa, Ine ngakhale manja anga, ndafunzulula Kumwamba , ...Yang’anani kwa Ine, kuti mupulumutsidwe inu malekezere onse a dziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibenso wina.*” Powerenga ndime zimenezi makamaka yomalizirayo, tiwona kuti Mulungu akutitsimikizira kuti Iye alipo ngakhale mu maonekedwe

eni eni kotero anthu onse ayenera kuyang'ana kwa Iye ndi maso a chiyembekezo komanso chikhulupiriro. Titsamize mutu wathu pa chiyembekezo chimenechi motero, tidzawerengedwa pamodzi ndi anzathu polandira mphothoyo ya Ufumu padziko lino lapansi.

-Namalenga anatiwululira kuti ali wachisoni ndi wokhululuka Iye amalankhulanso kwa anthu ake. Tiyeni tione ndi kuzindikira kuti chikhululukiro ndi chilankhulo chimachokera mu maganizo a umunthu. Nyama simakhululuka kapena kulankhula pamene ife anthu timatha zonsezi popeza tinapangidwa mu chifanizo chake cha Iye wolankhula ndi wokhululuka. Choncho, Davide anali wapamtima pake pa Yehova (Samueli 13:14) kuwonetsa kuti Munthu alinso ndi maganizo ngakhale kuti maganizo ake ndi osafanana ndi Yehova Namalenga. “*...Ndipo Yehova anamva chisoni chifukwa anapanga munthu padziko lapansi ndipo anabvutika mu mtima mwake*” (Genesis 6:6). Mulungu apa akubvutika chifukwa mu maganizo mwake sanayembekezere kuti munthu angachite zimene akuchita lerozi. Zomwe ife lero timachita zitha kukwiyitsa kapenanso kusangalatsa Mulungu, ngakhale kuti Iye Mwini amafunitsitsa kuti tiziwonetsa zizindikiro za Umulungu mu makhalidwe ndi m'maonekedwe athu chifukwa anatilenga ife m'chifaniziro ndi mu maonekedwe ake monga mwana ali kwa bambo wake. Koma m'malo mosangalatsa Iye amene ali Mlengi wathu, timamukwiyitsa kotero, ndi zomvetsa chisoni kwambiri. Mulungu ali wachisoni ngakhale izi zimamukwiyitsa amatipirira chifukwa Iye saali wodzikonda koma amafuna ife tidzisankhire tokha njira zathu, mwatsoka, timasankha chiwonongeko. Tizindikire kuti tiri ndi mwayi chifukwa mau tiri nawo pakati pathu.

TIYEREKEZE KUTI MULUNGU SAONEKA NGATI MUNTHU

Ngati Mulungu sangaoneke monga munthu awonekera; kungakhale kobvuta kwambiri kuti munthu'yo abvomereze ndi chikhulupiriro kuti Iye alipo ndiponso ngati alipodi amakhala bwanji? Baibulo limatiwuza kuti Mulungu'yo amakhala monga anthu aliri koma a khristu ambiri, chifukwa

chosawerenga mofatsa ndikusamvetsa zomwe Baibulo limanena pankhaniyi, samadziwa izi, kotero, ndichosadabwitsa kuona kuti akhristu'wo amakhala patsogolo mu uchimo. Munthu yemwe alibe luntha lodziwa za chinthu chirichonse monga tchimo, sangathe kugonjetsa bwino tchimolo chifukwa sakulidziwa komanso chifukwa china chikhoza kukhala kuti ngati amadziwa, ndiye kuti samalidziwitsitsa m'magonero mwake. Zotsatira za kusadziwa zambiri zokhudza Mulungu ndizakuti munthu osadziwa'yu sangathe kumuona Mulungu mu chikhalidwe chake, maonekedwe ake; sangakhale ndi chithunzi thunzi chake, chifanizo chake ndi *“pa Mpando Wa chifumu”* Wake monga Baibulo limafotokozera. Munthu otere sangathenso kuzindikira kuti iye akudetsa chikhalidwe ndi maonekedwe a Mulungu ndipo amakakamira pa zinthu ndi zikhulupiriro zopanda mutu weni weni. Mulungu anatipatsa kale mphamvu yake kotero sangalore kuti ife tiononge mphamvu ya chilengedwe mwaife pachifukwa choti tilandira *“Mzimu Woyera”* woti utithandize kuti tisachimwe ayi.

Tidziwe apa kuti sakuchimwa ndi Mulungu choncho, ngakhale ife tikuchimwa, m'malo moti ife tilape lero sitikuchitapo kanthu pakhalidwe lathu mu uchimo wathu. Kotero, zimakhala ngati kuti tikulandira chipulumutso chosakhetsera thukuta, (pogwira ntchito yake ya chiyero) zomwe zikusiyana kwambiri ndi chikonzero cha Mulungu choti aliyense waife alandire chipulumutso kapena chilango mogwirizana ndi zimene anafesa kapena kutengulira (kugwira ntchito yolemetsa ya chiyero poyesa yesa kuchita monga mwachifuniro chake). Ife tiyenera tichite monga Iye Mwini afuna ife tichite potengera chitsanzo cha khalidwe ndi maonekedwe ake omwe timawerenga mu Baibulo kuti ndi ofanana monga ife tiwonekera ndipo izi anazionetsa mwa Yesu Khristu pamene anabadwa padziko lapansi lino. Tikachita ichi, tidzaloledwa pamaso pake mu chiyero chake, ndikutinso Iye adzatilandira.

Cholinga cha Namalenga ndicho kuonetsa maonekedwe ndi makhalidwe ake kudzera mwa anthu ake omwe amamumvera pochita chifuniro chake'cho. Dzina lake la chikumbutso pakati pathu ndilo Yehova Eloimu lomwe litanthawuzira *“Iye odzakhala Akulu Ambiri Iwo”* Tiona kuti ngati Mulungu sangaoneke ngati momwe ife timaonekera (monga Khristu

ankaonekera!) ndiye kuti mphotho ya akhristu okhulupirira siyidzaonekanso. Pamene mphotho ya Ufumu Wa Mulungu monga Baibulo limanenera, ndimoyo wosatha mu Ufumu Wa Mulungu Umene'wu; anthu ambiri omwe amati ndi akhristu, saali okonzeka kuulandira m'maonekedwe eni eni popeza munthu ndi ofooka, ochedwa ndi maganizo ake a uchimo. Yobu akukamba za *"masiku otsiriza"* tsiku lomwe iye anakhulupirira kuti adzafika Iye (Yesu); Yobu apa anali ndi chiyembekezo choti adzawuka kwa akufa (Yobu 19:25-27); Abrahamu ndi m'modzi mwa *"...ambiri a iwo ogona mpfumbi lapansi (omwe) adzawuka, ...kumka ku moyo wosatha"* (Danieli 12:2) kotero, adzalandira zotsatira za lonjezo la mphotho ya dziko lamuyaya la Kanani, lomwe ndi mbali yeni yeni yadziko lapansi (Genesis 17:8). *"...Ndipo ansembe (saints?) ake ndidzawabveka ndi chipulumutso; ndi okonedwa ake adzapfuulitsa ndi chikondwerero; ...apfuule mokondwera pamakama pao; ndikupereka chilango m'chiweruzo cha ochimwa"* (Masalmo 132:16; 149:5,7). Kusamvetsa ndi kusakhutira ndi mfundo zimene'zi za malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu omwe timawerenga mu Baibulo, pakati pa a Yuda ndi a mitundu, ndikumene kumabweretsa chikhulupiriro cha bodza cha mzimu wosafa mwa anthu a padziko. Maganizo amene'wa a umunthu kukhala ndi mzimu m'thupi mwake samapezeka paliponse mu Baibulo ndipo yense okhulupirira izi alibe gawo pa chipulumutso cheni cheni cha Mlengi Wathu. Chiuta ndi wa Ulemerero, wosafa mpaka muyaya, komanso ali ndi cholinga ndi dziko lonse, kotero, abambo ndi amayi onse akuyitanidwa kubwera kwa Iye kukakwaniritsa cholinga chake'cho, kuti akapatsidwe Ufumu Wa Mulungu womwe udzakhazikitsidwe padziko lino lapansi. Zonse'zi monga timawerenga, zinawonetsedwa kwa okhulupirira anzathu kalelo mu umunthu omwe ndi chifaniziro chake.

Mwayi ulipo kwa okhulupirira onse kuti adzalandire udindo wolamulira chilengedwe chonse mwa Umulungu (2 Petro 1:4). Pamene anthu ena akuganiza kuti chipulumutso chimabwera munthu atalandira Mzimu Woyera, sizimamveka chifukwa ngakhale Baibulo silinenapo mfundo yotere kotero, anthu m'mipingo yambiri anapanga mbiri yawo yawo yomwe ilibe gawo m'Buku Lopatulika. Mwaichi, anatengerapo mwayi powonetsetsa kuti kumasulira Buku Loyera'li kuchokera mzilankhulo zina kukhale

kogwirizana ndi m'mene iwo amaganizira. Ife tikawerenga Baibulo, malo ambiri amatitsimikizira kuti tidzapatsidwa thupi monga la Yesu (Filipo 3:21) kotero, tidziwanso kuti Ambuye Yesu ndi ife tonse, tidzakhala ndi thupi leni-leni tiri naloli mu Ufumu Wake, tidzakhala ndi thupi ndi maso, makutu, manja, zipsera ndi miyendo (Zekariya 13:6; Yesaya 11:3). Tawerenga kuti aliyense waife analengedwa mu chifaniziro cha Mulungu kotero tikaona anzathu ena onse, ndiye kuti tawona chithunzi thunzi cha Mulungu choncho, tiyeni tiwalemekeze ndi kuwakonda anzathu omwenso ndi maonekedwe ake mu chiyero. Tiyenera kugwirizana ndi chilimbikitso cha *“Uthenga Wabwino”* wopezeka m'Buku Lake omwe unalembedwa ndi cholinga chimene'chi.

Taona mfundo imodzi mu phunziro lino yoti Chiuta ndi anthu ake amaoneka mofanana kupatula nzeru (chikhalidwe) zake zomwe ndi zosiyana ndi ife anthu. Chimene tichite panopa n'kusakasaka chikhalidwe chenicheni cha Mlengi'yo kotero kuti tikayandikire kufupi ndi Iye podziwa chikhalidwe chake'cho. Tiyese-yese kuchita chifuniro chake poteteza chikhulupiriro chathu mwa Iye, mwanjira iyi, tikakwaniritse cholinga chake'cho pobvala mawonekedwe ndi makhalidwe akewo. Ife lero ndife olimbikitsidwa popeza tikupindula kwambiri pokhala ndi Atate athu achikondi, amene amatidzudzula ngati momwe bambo adzudzulira mwana wake (Deuteronomo 8:5). Tikawerenga za mazunzo a Yesu Khristu, timva kuti: *“...kunakomera Yehova kumtundudza; anam'mvetsa zowawa”* (Yesaya 53:10), *“...ngakhale kuti Mkusauka Kwanga Ndinaitana Yehova, Ndipo Ndinakuwira Mulungu wanga; Mau anga anawamva m'kachisi mwache”* (Masalmo 18:6). Mulungu atalonjeza Davide kuti adzakhala ndi mwana yemwe adzatchedwa *“Mwana Wa Yehova”*, Zinali zomveka kuti mwana'yo abadwe m'njira yomwe aliyense sanayembekezere; pakanakhala kuti Mlengi sali ngati munthu, kukanabvuta kuti mwana'yo (Yesu) abadwe m'njira yotere m'maonekedwe a munthu koma okhala ndi chikhalidwe cha Mulungu.

Tikamvetsetsa bwino ndi kuzindikira momwe Mulungu aliri ndi makhalidwe ake, timakhala ngati makiyi (akabali) otsekulira zitseko za kazindikiridwe ka mfundo zina za Mau a Mulungu. Tiona kuti pamene

mabodza okhudza Mau Oyera ndi maonekedwe a Namalenga ayamba kusanjikizana, amatsekereza zowona zenizeni za *“Uthenga Wabwino”* omwe Mau a Mulungu angapindulire munthu. Mwina n’kutheka kuti mwapindulapo kanthu pagawo lino, mfunso lalikulu ndi lokupemphani kuti tifufuze bwino zambiri za Iye mu Buku Lopatulika kuti tikhale ndi chithunzi-thunzi chabwino cha Iye kotero, tikampembedze kokwanira ndi nzeru zathu zonse.

1.3 DZINA LA MULUNGU NDI MAKHALIDWE AKE

Timakhulupirira kuti kudziko kuno kuli Mulungu, ndipo Chauta wathuyo ayenera kuti anakonza kale njira yotiphunzitsira kapena tinene kuti yotiwuza zambiri zokhudza Iye. Ife timadziwa kuti njira imene’yi ndiyo *“Baibulo”* lomwe ndi Mau ndi chitsimikizo chake pakati pathu, kotero, Mulungu Mwini’yo amadziulula m’makhalidwe ake kudzera Mu mau ake omwe timawerenga m’Buku Lopatulika. N’chifukwa chake Mau ake akutchulidwanso *“Mbeu Yake Yosawola”* (1 Petro 1:23); mwaichi, tikatsutsidwa ndi zochita zathu poyerekeza ndi zomwe Mau ake akutiphunzitsa, timabadwanso mwatsopano pobvala makhalidwe a Umulungu omwe tawuphunzira mu Mau ake’wo (Yakobo 1:18; 2 Akorinto 5:17). Munjira iyi, tikalimbikira, ndikuyesetsa kuzindikira Mau a Mulungu, tikaphunzira kukhala ngati Namalenga komanso ngati Mwana Wake Yesu Khristu popeza ndiye chitsanzo chake cheni-cheni. Ifenso *“timasanduka chitsanzo chake cha Mulungu pakati pa anthu anzathu”* (Aroma 8:29). Makhalidwe ake aYesu, anali chifanizo ndi chitsanzo cha Yehova Mulungu wathu (Akolose 1:15). Motero, ife timayenera kuwerenga kwambiri mbiri yake mozama mu Baibulo, momwe tingamvetse bwino zomwe Mulungu anawonetsa pa chiweruzo ndi malongosoledwe a chikhalidwe choyenera pakati pa anthu mu mayiko mwawo. Baibulo ndiye muuni wathu pa chikhulupiriro chirichonse mu moyo wachikhristu kotero, tidzakhala chifanizo ndi chitsanzo kwa anzathu tikatsata chiyero cha Mau ake.

Mu chi Hebri, dzina la munthu kalelo, mogwirizana ndi chipembedzo chawo, linali ndi tanthauzo lokhudzana ndi chikhalidwe kapena mbiri yake kuphatikizapo zolinga za munthu'yo. Zitsanzo ziri m'munsi'zi ndi amodzi mwa mayina omwe anzathu a chi Hebri anakonda kupereka kwa ana awo:

“Yesu” (“Mpulumutsi”) “...chifukwa adzapulumutsa anthu ake kumachimo awo” (Mateyu 1:21)

“Abrahamu” “Bambo wa namtindi wa anthu” “chifukwa kuti ndakupanga iwe kukhala atate a khamu la mitundu ya anthu m'mayiko” (Genesis 17:5).

“Hava” “Wamoyo” “chifukwa ndiye amake wa amoyo onse” (Genesis 3:20).

“Simeoni” “Wakumva” “...chifukwa anamva Yehova kuti anandida ine, anandipatsa mwana wamwamuna uyu” (Genesis 29:33) Mwana opatsidwa m'chisomo chake cha Mulungu.

Yeremiya 48:17, **“Kudziwa zambiri za dzina lake ndi anthu a Moabu kufanana ndi kudziwa zambiri za mfumu ya a Moabu.”**

Tikawerenga (Masalmo 103: 1; 105:1; 106:1,2,12,13) Mulungu akudziwika ndi dzina lake, Mau ake ndi ntchito zake. Choncho, maina a Mlengi wathu, mayina a ma uundo wake ayenera kutiuzza zambiri za Iye. Tikudziwanso kuti pali zinthu zambiri zomwe zikukhudza makhalidwe ndi cholinga cha Mulungu, ndipo kuti ali ndi mayina ambiri mbiri. Phunziro lapadera lokhudza dzina la Mulungu liripo koma ndibwino kuphunzira phunziro'li munthu atabatizidwa kale ndi cholinga choti alimvetse bwino; munthu akhonza kukhutitsidwa ndi makhalidwe komanso cholinga chake pokha pokha ngati atapitiriza kuwerenga pa moyo wake onse mwa Khristu. Kotero, zomwe tikuphunzira pano ndi chiyambi chake cha maphunziro'wa.

Mose pofuna kuwonjezera nzeru zake, kudziwa zambiri ya Mulungu, polimbitsa chikhulupiriro chake pa nthawi yobvuta ija, mu Ngelo anamuwonekera nanena **“...Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wachisomo, wolekerezana ndi wokoma mtima kochuluka, ndi wachoonadi; wakusungira anthu osawerengeka chifundo chozama, wakukhululukira mphulupulu ndi kulakwa ndi kuchimwa; koma wosamasula wopalamula; wakulangira ana ndi zidzukululu chifukwa cha mphulupulu ya atate awo...”** (Eksodo 34:5-7).

Apa ndi zowonekeratu kuti mayina onse a Namalenga akuwonetsa umoyo ndi cholinga chake. Pokhala Mwini zonse, ndiye kuti alipodi mu uthunthu wake wonse womwe sungawonekere mu mzimu (mphamvu) wokha koma zochitika za tsiku ndi tsiku. Akafuna amatha kuonekera kwa anthu mu uthunthu wakewo. Mulungu anasankha dzina lake limodzi lokha lomwe ife timamudziwa nalo ndiponso Iye Mwini afuna tizilikumbukira nthawi zonse. Mwachidule, ndi dzina komanso chizindikiro cha cholinga chake pa anthu ake onse m'dziko.

Ana amfuko la Israeli anali akapolo ku Aigupto ndipo kunali koyenera kuwakumbutsa zambiri za cholinga cha Mulungu pa iwo. Mose anawuzidwa kuti awakambire iwo za dzina la Mulungu kotero kuti analimbikitsidwa kuchoka mu dziko'lo ndikuwuyamba ulendo wopita ku dziko lawo la malonjezano (1 Akorinto 10:1). Kudziwa dzina la Yehova ndi tanthawuzo lake ndi kofunika kwambiri. Ifenso tiyenera tizindikire dzina la Mlengi Wathu ndi tanthawuzo lake tisanabatizidwe poyamba ulendo wathu wopita ku **“Ufumu wa Mulungu”** Ngati sitidziwa tanthawuzo la dzina la Yehova Mulungu Wathu, komanso ngati sitimudziwa Iye mwapadera, sitingathe kudzipereka pa **“Ulendo Wathu wopita ku Ufumu Wake”** popeza tiri osamudziwa Iye, osazindikira zolinga ndi zofuna zake.

Chiuta anawauza ana a Israeli kuti dzina lake ndi **“YAHWEH”**; kutanthawuzira kwake ndiko kuti, **“INE NDINE YEMWE NDIRI INE”** kutanthawuzira kweni-kweni ndiko kuti **“INE NDINE YEMWE NDIDZAKHALA INE** (Eksodo 3:13-15). Dzina linakuzidwa: **“...Mulungu ananenanso** (i.e. mowonjezera) **kwa Mose, ukatero ndi ana a Israeli: Yehova, Mulungu wa makolo anu, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi Mulungu wa Yakobo wandituma kwa inu; ili ndi dzina langa nthawi yosatha, ichi ndi**

chikumbukiro changa m'mibadwo mibadwo...” (Eksodo 3:15). Mibadwo mazana mazana lero yakhala ikudziwa ndipo imadziwabe dzina la Mulungu. Choncho, dzina lonse la Chiuta, Mulungu Wathu, ndi *“Ambuye Ndiye Mulungu”*. Palibe dzina lina lirilonse loposa ili kotero tiyenera kulimbikitsidwa.

Chipangano Chakale kwambiri chinalembedwa mchilankhulo cha chi-Hebri, apa ndi zowonekeratu kuti Baibulo la zilankhulo zina zochokera mu chizungu ndi zilankhulo zina silingapereke matanthauzo onse ndi makhalidwe owona a Mulungu. Ichi ndi chifukwa choti otanthauzira Mau a Mulungu ambiri (makamaka chichewa) ankanthawuzira molingana ndi momwe iwo eni ankafunira mu malo mopereka tanthauzo lomwe liyenera kuperekedwa kuti chiganizo chimveke monga chinalembedwera. Potanthawuzira Mau a Mulungu, sitienera kutanthawuzira kuti zigwirizane ndi maganizo kapena zolinga zathu ayi koma kuti munthu akawerenga, amve ndi kuzindikira maganizo, makhalidwe ndi zolinga za Mulungu. Chitsanzo chachikulu ndi munthu yemwe amatha kuwerenga Baibulo la Chi Hebri amawonera kusiyana ndi ma Baibulo a zilankhulo zina. Mfunso lingakhalepo ndi loti, ngati ziri choncho kodi ife tingalandire chipulumutso cheni cheni potsamira chikhulupiriro chathu pa zinthu zabodza? Kodi kusiyana kwa mamasulidwe kumeneku kunabwera chifukwa chiyani? Kodi kumasulira Baibulo kunachitika mogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu kuti cholinga chake ndi Mulungu chidziwike. Dzina limodzi la Mulungu mu chi Hebri lomwe linamasulidwa kuti **“Mulungu”** ndi **“ELOHIM”** pamene tanthauzo lake leni leni ndiye **“Amphamvu ambiri”**. Dzina la **“Chikumbutso”** kwaife kuti tizimukumbukira kotero, liyenera kukhala **“YAHWEH ELOIMU,”** kutanthawuzira kwake koyenera kungakhale **“IYE YEMWE ADZAMVEKA MGULU LA AMPHAMVU ONSE”**. Iri ndilo dzina lomwe Mulungu ayenera kudziwika nalo lomwense ndi dzina la matanthawuzo palokha. Mu dzina’li tikhoza kupezamo maphunziro ambiri okhudza ntchito ndi cholinga cha Mulungu.

Kotero, cholinga cha Mulungu ndicho kuwonetsa komanso kumveketsa khalidwe, umoyo ndi zochita zake pakati pa anthu ambiri. Ife tikamvera Mau ake tikhoza kukula mu chikhalidwe, umoyo ndi ntchito zake ndipo kuti izi zikaonekere ndi kutitsimikizira kwa Iye, zikadziwitsenso kuti Mulungu’yo alipo pakati pa anthu omwe ali pafupi ndi ife ndikuti ifenso pamodzi ndi anthu’wo

tonse tazindikiradi, tidzakula mu moyo wa chisomo chake. Onaninso kuti dzina la Mulungu ndi mlozo olosera zakubwera kwa nthawi irinkudzayo pomwe dziko lapansi lidzadzaza ndi anthu omukonda Iye mu uthunthu wa Umulungu wake komanso mu khalidwe, umoyo ndi ntchito zake (2 Petro 1:4). Ngati ife tifuna kukhala ndi mbali ndinso cholinga chake cha Chiuta, ndi kukhalanso ngati Iye amakhalira wamuyaya, osafa, kukhala a moyo mpaka muyaya, opanda banga, tiyenera kukhalanso ndi mbali mu dzina lake pochita zomwe Iye afuna ife tichite. Njira yabwino yokwaniritsa izi ndiyo kubatizidwa mu dzina lake i.e. **“Yahweh Eloimu”** (Mateyu 28:19). Tikatero, tidzakhalanso ndi mwayi otchulidwa **“Mbeu”** kapena **“ana a Mulungu”** (Agalatiya 3:27-29) omwense analandira malonjezano opatsidwa ulamuliro wa dziko lonse lapansi (Genesis 17:8; Aroma 4:13) – kukhalanso amodzi mwa gulu la **“Amphamvu onse (Eloimu)”** Omwe adzakwaniritse mlozo wa dzina la Mulungu. Kodi ndani waife amene sangasangalale ataona kuti wasankhidwa nawo kukhala m’gulu limeneri? Tiyeni tiziyesetsa kuchita chifuniro chake kuti tikhale amodzi mwa iwo. Tikalandira ufulu umenewu, tidzakhala ndi chisangalalo chosaneneka kotero, anzathu onse omwe akunyozera pochita ichi, adzasirira. Mulungu naye amasangalala ngati munthu yemwe ali chinyezimiro chake achita zomukondweretsa Iye. Tiphunzira zambiri za izi Mphunziro 3.4.

1.4 ANGELO

Zonse zomwe tawona tsopano mu Phunziro lino zatipatsa mwawi ndi luntha lofuna kudziwa zambiri za Angelo:

- mu umunthu ndi uthunthu wawo
- wonyamula ndi kukweza dzina la Mulungu
- Ngati njira zomwe mphamvu ya Mulungu (Mzimu) zimadzera pokwaniritsa kuchita zofuna zake

-mogwirizana ndi khalidwe, umoyo ndi cholinga cha
Mulungu

-mwaichi, ntchito zake mwa umunthu ziyenera kuonekeranso

Takambapo m'phunziro 1.3 kuti liwu la mu chi Hebri, lomwe linanthawuzidwa kuti **“Mulungu”** kwambiri ndilo **“Eloimu”** ndipo tanthauzo lake leni leni ndi **“Amphamvu ambiri onse”** koteru **“Amphamvu ambiri onse”** amenewa omwe amakweza dzina la Mulungu akhoza kutchulidwanso **“Mulungu”** chifukwa amakhala pafupi ndi Iye. **“Amphamvu ambiri onse”** amenewa ndiwo **Angelo**. Ndi amodzi mwa a **“Eloimu”**.

Mbiri ya chilengedwe cha dziko mu Genesis 1, imatiwuzwa kuti Mulungu analamula kuti zinthu zonse zilengedwe **“ndipo kunatero”**. Tikawerenga mozama Mau ake, tidzawona kuti ndi Angelo omwe ankagwira ntchito yaikulu ya chilengedwe pomvera malamulo a Mulungu'wo:

“Lemekezani Yehova, inu angelo ake, A mphamvu zolimba, akuchita Mau ake, Akumvera liu la Mau ake.” (Masalmo 103:20).

Chotero, ndikoyenera kukhulupirira kuti pamene timawerenga za Mulungu kuti analenga dziko (Angelo analengedwa ndi Mulungu), ntchito yeni-yeni yolengayo inagwiridwa ndi Angelo. Yobu 38:4-7 akubvomereza mfundo yomweyi ya chilengedwe. Mu Buku loyamba la Genesis 1:

-Tsiku loyamba “...Mulungu anati, kuyere: ndipo kunayera” (ndime 3)

-Tsiku lachiwiri “...Mulungu anati, pakhale thambo pakati pa madzi, lilekanitse madzi ndi madzi. Ndipo Mulungu anapanga thambo, nalekanitsa madzi anali pansu pa thambo ndi madzi anali pamwamba pa thambo: ndipo kunatero (ndime 6,7).

- Tsiku lachitatu** “...Mulungu anati, madzi a pansi pa kumwamba asonkhane pamodzi pamalo amodzi, uoneke mtunda: ndipo kunatero” (ndime 9).
- Tsiku lachinayi** “...Mulungu anati, pakhale zowunikira pathambo lakumwamba, zakulekanitsa usiku ndi usana; zikhale zizindikiro ndi nyengo, ndi masiku ndi zaka...ndipo kunatero...” (ndime 14,15)
- Tsiku lachisanu** “ Mulungu anati, madzi abale zochuluka zamoyo zoyenda yenda, ndi_mbalame ziuluke pamwamba pa dziko lapansi ndi pa mlengalenga Mulungu ndipo analenga zakuchuluka ndipo kunatero...” (ndime 20,21).
- Tsiku lachiweru** “... Mulungu anati, dziko lapansi libale zamoyo monga mwa a mitundu yawo, ng’ombe, ndi zokwawa...ndipo kunatero” (ndime 24-25).

Munthu analengedwa tsiku lachisanu ndi limodzi. **“Mulungu anati tiyeni tipange munthu m’chifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu:”** (Genesis 1:26).

Mvetsetsani liwu loti **“kupanga”** osati **“kulenga”**. Takamba zambiri pandime iyi m’phunziro 1.2 . Pakali pano, tikufuna tiwonetsetse ndikuzindikira kuti **“Mulungu”** pa ndime iyi sakukamba za Iye yekha pamene ankapanga munthu. **“..Tiyeni tipange munthu..”**apa Mulungu akunena za alengi ambiri osati m’modzi ayi.Tsono ngati alengi amenewa anali ambiri Mulungu ana-phatikizapo ndani polankhula zimenezi?

N’chifukwa chake mau awa m’Baibulo, liwu limene lagwiritsidwa ntchito ndi lomwe lija la “Eloimu” lotanthawuzira “Amphamvu ambiri onse”ndipo zikuwonetseratu kuti Mulungu amaphatikizanso “Angelo” pameneananena izi. Ngakhale ife tinalengedwa ndi Angelo molamulidwa ndi Chiuta mu chifanizo chake, chomwenso chiri chifanizo cha Angelo, maonekedwe athu ndi

angelo ndiwofanana popeza tonse ndife olengedwa m'chifanizo chake cha Mulungu. Thunthu lathu ndi chifani-fani cheni-cheni cha Mlengi Wathu koma ife anthu tinapatukana ndi Angelo chifukwa cha tchimo. "Maonekedwe ndi makhalidwe a chilengedwe" tatchulawa akukhudza kwambiri momwe anthu ndi angelo amawonekera ndi makhalidwe awo mu uthunthu wao (thupi). M'Baibulo, muli maonekedwe ndi makhalidwe a mitundu iwiri ndipo ife sizingatheke kukhala ndi mitundu iwiri yonse'yi nthawi imodzi maka pano pamene Ambuye Yesu sanabwere kudzaweruzza dziko lapansi.

CHIKHALIDWE CHA MULUNGU (CHIYERO)

- Opanda banga (olungama) (Aroma 9:14;6:23; cp. Masalmo 90:2; Mateyu 5:48; Yakobo 1:13)
- Sangafe (ali ndi moyo wamuyaya) (1 Timoteo 6:16)
- Ndi Wamphamvu zochuluka (zopanda malire) (Yesaya 40:28).

Awa ndiye mawonekedwe komanso makhalidwe a Chiyero a Mulungu ndi Angelo ndipo makhalidwe amenewa, anapatsidwanso kwa Yesu Khristu atawuka kwa akufa (Machitidwe 13:34; Chibvumbulutso 1:18; A Hebri 1:3). Ife tikakhulupirira tidzalandiranso mphotho yapamwamba ya maonekedwe ndi chikhalidwe chotere'chi monga mwamalonjezano ake (Luka 20:35,36; 2 Petro 1:4; Yesaya 40:20 cp.ndime 31).

CHIKHALIDWE CHA MUNTHU

- Choyesedwa ndi machimo (Yakobo 1:13-15) moyo wodzala ndi maganizo a uchimo ([mtima wakuda] [Yeremiya 17:9; Marko 7:21-23])
- Wotembereredwa ndi imfa ([mu chibadidwe] [Aroma 5:12,17; 1 Akorinto 15:22]).

- Chiri ndi mphamvu zoperewera ndi zofooka mu chikhalidwe (Yesaya 40:30) komanso m'maganizo (Yeremiya 10:23).

Chikhalidwe cha munthu ndi chosalongosoka, inde alipo ena abwino koma ambiri ndi oyipa, operewera kwambiri pamaso pa Namalenga. Khalidwe lililonse liri ndi mapeto ake. Ochimwa malire awo ndi imfa (Aroma 6:23). Chikhalidwe cha uchimo ndi chimene Yesu Khristu anali nacho mu chibadidwe ngakhale sanali ochimwa (A Hebri 2:14-18; Aroma 8:3; Yohane 2:25; Marko 10:18). N'chifukwa chake anali ofooka ndi odandaula nthawi zina, monga pamene anapachikidwa pa mtanda, analira. Tikati chikhalidwe, sitikunena chikhalidwe kapena maonekedwe monga timagwiritsa ntchito m'moyo wathu watsiku ndi tsiku ayi koma ngati momwe Baibulo lifotokozera pakati pa thupi ndi chiyero, tchimo ndi ungwiro.

CHIKHALIDWE NDI MAONEKEDWE ANGELO

Mchifanizo cha Mulungu, nawonso Angelo sachimwa kotero sangathenso kufa popeza *“mphoto yauchimo ndi imfa”* (Aroma 6:23). Angelo ndithu amaoneka ngati momwe ife tionekeka, uthunthu wao ndiofanana ndi anthu. Chifukwa chaichi, takhala tikuwerenga kuti kale pamene angelo ankawonekera kwa anthu pansi pano, anali kutchulidwa anthu powona kuti palibe kusiyana ndi anthu'wo m'maonekedwe awo. Kotero, tiyenera kutsata ndi kumvera zomwe Mau A Mulungu amatiuzira ndipo izi zimagwirizana ndi m'mene timaonera Buku Lopatulika molingalira zolinga zathu pa chipulumutso.

-Angelo atampeza Abrahamu, anamuwuzza zomwe Mulungu anawatuma iwo. Apa tiona kuti anatchulidwa *“anthu atatu”* omwe poyambapo Abrahamu anawaona ndikuwatenga ngati anthu wamba chifukwa cha maonekedwe awo: *“...ndikupemphani, nditengetu madzi pang'ono, ndikusambitseni mapazi anu, mupumule pansi pamtengo ...”* (Genesis 18:2-4). Mulungu anayikiratu ndondomeko ya chilengedwe choti chisasiyane pakati pa Iye ndi chilengedwe chimene Iye anachipatsa udindo padziko.

-Awiri mwa Angelo amene'wa anapita kwa Loti mu Mzinda wa Sodomo. Ukunso, anawatenga ngati anthu wamba onse Loti ndi anthu a mu Mzinda'wu:- *“Ndipo anadza mu Mzinda wa Sodomu a mithenga awiri”* omwe Loti anawayitana. Koma anthu a mu Mzinda wa Sodomu anabwera kunyumba kwa Loti moopseza *“...ali kuti anthu amene anadza kwaiwe usiku uno? Utitulutsire tiwadziwe...”* Loti anawapempha, *“...anthu awa*

musawachitire iwo choyipa...” Mau a Mulungu nawo akutchula angelo’wa **“anthu”**: **“...Koma anthu aja** (angelo) **anatulutsa dzanja lawo** (anthu awiri anali ndi dzanja limodzi?)” Ndipo timva kuti anamupulumutsa Loti; **“...ndipo anthu aja anati kwa Loti...ndipo Yehova anatumiza ife kudzawononga Sodomo popeza sakondwera ndi zochita zawo”** (Genesis 19:1,5,8,10,12,13).

-Chipangano Chatsopano pophera mphongo mauwa, chikutsimikizira kuti angelo ndi ofananadi ndi uthunthu wa anthu mu maonekedwe: **“...musayiwale kuchereza alendo; pakuti mwaichi, ena** (monga Abrahamu, Loti, etc) **anachereza Angelo osachidziwa....”** (A Hebri 13:2).

-Yakobo analimbana naye munthu kufikira mu mbandakucha ([panjira] Genesis 32:24), ndipo timawerenga kuti munthu uyu anali M’ngelo (Hoseya 12: 4).

-Anthu awiri obvala zobvala zoyera zonyenzimira anawoneka pamene Yesu anawuka kwa akufa (Luka 24:4) ndi pamene Yesu anakwera kumwamba (Machitidwe 1:10). Tiyenera kudziwa mosakayika kuti onsewa anali Angelo ngakhale adaoneka ndi zobvala ngati anthu.

-Tangoganizani za **“muyeso wa munthu, ndiye M’ngelo.”** (Chibvumbulutso 21:17)

ANGELO SAMACHIMWA

Angelo omwe ndi chifanifani cha chikhalidwe cha Mulungu, sangafe. Monga tidziwa kuti tchimo limabweretsa imfa, angelo samachimwa komanso mwaichi, sangafe. Mau a chi Hebri ndinso chi Greek amene atanthauzidwa **“Angelo”** matanthauzo ake eni-eni ndiye kuti **“Mtumiki”**; kotero, angelo ndi atumiki kapena tinganenenso kuti **“antchito”** a Mulungu, omumvera ake, motero n’kobvuta kwambiri kuti angelo angakhale ochimwa. Motero, liwu lachi Greek loti “aggelos” lomwe mu Baibulo linanthauzidwa **“Angelo”** limanthauzidwanso **“Atumiki”** pokamba za anthu omtumikira Iye, mwa chitsanzo Yohane **“M’batizi”** (Mateyu 11:10) ndi atumiki (Luka 7:24); Atumiki a Yesu (Luka 9:52) ndinso anthu amene anazonda Mzinda wa Yeriko (Yakobo 2:25). Tionanso kuti anthu eni eni okhawo omwe atchulidwa Angelo kapena titi **“atumiki a Mulungu”** ndi omwe angachimwe. Chifukwa chakuti Angelo amakhala mu ulemmerero wa Mulungu asiyaniratu ndi utumiki wathu wochita mu machimo. Manunsu otsatira’wa akutiuzwa za Angelo onse (osati ena

mwaiwo monga satana ayi) kuti mwachilengedwe chawo ndi omvera Mulungu cho'ncho, sangachimwe ndipo kuti sanachimweponso:

“...Yehova anakhazikitsa Mpando Wake Wachimfumu M'mwamba; ndi Ufumu Wake Uchita Mphamvuponse-ponse (mwachitsanzo, palibe yemwe angagalukire kapena kuukira Ufumu Wake M'mwamba chifukwa Iye ndi Wamphamvu zoposa mphamvu zina zonse), **Lemekezani Yehova, inu Angelo ake, a mphamvu zolimba, akuchita Mau Ake, Akumvera liwu la Mau Ake. Lemekezani Yehova, inu makamu Ake onse; Inu atumiki Ake akuchita chomukondweretsa Iye...**” (Masalmo 103:19-21).

“...Mlemekezani, Angelo Ake onse; mlemekezani makamu ake onse...” (Masalmo 148:2).

“...za AngeloKodi si Iwo otumikira anthu mwamphamvu, otumidwa kulalika kwa iwo (okhulupirira) omwe adzalandire udindo wa Chipulumutso...” (A Hebrai 1:13-14).

M'malo ambiri, tikuwerenga kuti **“Angelo”** onse kutanthauza kuti palibe magulu angapo a Angelo. Palibe zoti pali angelo oyipa kapena abwino ayi. **“Onse ndi Angelo”** basi, otumikira osati oyipa kapena abwino ayi. Tiona kuti kuzindikira zambiri za maonekedwe ndi chikhalidwe cha Angelo, ndichinthu chothandiza kwambiri pamoyo wathu wa chikhristu chifukwa tingazindikire bwino kuti okhulupirira onse adzalandira mphotho yothandiza kukhala ndi chikhalidwe chawo. **“...Koma iwo akuyesedwa oyenera kufikira dziko lijalo, ...sawatira kapena kukwatiwa...komanso sangafenso pakuti afanana ndi Angelo”** (Luka 20:35-36). Mfundo iyi ndiyofunika kuyimvetsetsa kuti kuwerenga Baibulo kukhale ndi phindu kwaife m'moyo wathu. Angelo samafa: **“..imfa iribe ulamuliro pa iwo”**. Angelo akanakhala kuti amachimwa, zikanatanthauza kuti anthu onse omwe ali woyera pamaso pa Mulungu adzachimwa ngakhale chiweruzo chidzakhala chitachitika kale. Ndipo powona kuti mphotho ya uchimo ndi imfa (Aroma 6:23), kudzakhala kobvuta kwambiri kuti anthu alandire mphotho ya moyo wosatha, tinganenenso kuti moyo wosatha sungakhalepo! Choncho, tikanena kuti Angelo amachimwa, tikutsutsa malonjezano ndi chikhulupiriro choyenera cha Mulungu, cha moyo wosatha, pozindikiranso kuti mphotho yathu pa chikhulupiriro mwa Iye, ndimoyo wosatha ngati tidzakhala nacho chikhalidwe ndi maonekedwe a

Angelo. Tawona kuti “*Angelo onse*” (Luka 20:35-36) sakupatula Angelo ena ayi koma kunena za “*Angelo onse*” mosapatula chon’cho, payenera kukhala gulu limodzi lokha la Angelo osati magulu awiri (oyipa ndi abwino) ngati m’mene amanenera ena ayi. Zikanakhala choncho, Baibulo lidamakamba za magulu amene’wa koma silimafotokozapo za izi.

Ngati Angelo angachimwe, ndiye kuti Mulungu angakhale padera; opanda Mphamvu mu chilungamo; sangathe kukhala ndi ulamuliro m’miyoyo yathu ndinso kulamulira zochitika mu dziko lonse monga akuchitira panopa ngakhale ife sitimamvetsa bwino za Mphamvu zake lero; popeza timawerenga kuti amagwira ntchito yake kudzera mwa Angelowo (Masalmo 103:19-21). Angelo anapatsidwa mphamvu ndi Mulungu chifukwa Mulungu’yo ndi Wamphamvu, amachita zonse M’mphamvu zake’zo kudzera mwa Angelo ake (Masalmo 104:4).

Tadziwa tsopano kuti Angelo atsamira ndi kuwerengera zochita zawo pa Mphamvu ya Mulungu. Tiona kuti ngati Angelo alibe Mphamvu ya Mulungu, ndiye kuti sangathe kuchita chiri chonse, motero, inu, ine ndi Angelo onse, tonse tiri chabe; Koteronso tiyenera kuganizira bwino pa mfundo yoti Angelo sangamvere Mulungu. Chifukwa chaichi, ife timaona kuti sizingatheke kuti Angelo sadamverepo Mulungu monga akhristu ena amanenera za satana yemwe sanamverepo Mulungu; izi ndi zabodza, kubwereza bodza lomwe lija linachitika mu Edeni ndi njoka ija. Tikanena kuti Angelo samamvera Mulungu ndiye kuti tikuderera Mphamvu ndi Ungwiro wa Mulungu kuti sangathe kulungamitsa ndi kulungosola chilengedwe chake, n’chifukwa chake anthu ambiri amanena kuti satana wawachimwitsa ayiwala kuti tchimo limabwera chifukwa cha zofuna ndi chilakolako cha thupi lawo (Yakobo 4:17), osati kuwumirizidwa ndi satana. Mulungu ali ndi Mphamvu zomwe anaperekako kwa satanayo koteru, ndo kosabvuta kuti Mulunguyo achotse Mphamvu zakezo mwa satana.

Tiyeni tsono tizipemphera kwambiri kuti “Ufumu Wake Udze” padziko lino lapansi, pomwepo kuti kufuna kwake kukachitike monga Kumwamba chomwecho panso pano (Mateyu 6:10).

Zitakhala kuti Angelo a Mulungu amapikisana ndi Angelo ochimwa Kumwamba, zingabvute chifukwa kumwambako zonse zikuchitika mu ndondomeko molamulidwa ndi Mulungu yemwe ali Woyera opanda banga monga tawerenga m’mbuyomu; Kungabvute kuti cholinga chake

chikwaniritsidwe ngakhale mu Ufumu Wake Ulinkudzawo, kungabvute kuwuongolera kwake ngati Mulungu adalephera kuongolera zochitika m’masiku oyamba adanenedwawo. Uku ndi kungofuna kuchepetsa mphamvu zodabwitsa za Yehova Mulungu Wathu. Tiyeni tidzipereke pofuna kuzindikira zambiri za Mlengi Chiuta Wathu ndi nzeru zathu zonse. Tangoganizani inu, mukakhale mu “Ufumu Wa Mulungu” womwe mpaka pano kuli nkondo pakati pa satana (uchimo) ndi Mulungu chifukwa chakuti m’modzi mwa Angelo sanamvere, izi sizingatilimbitse mu chikhristu chathu popeza zikuoneka kuti Yehova ndi wolephera kukusa Angelo ake omwe ndi chinyezimiro m’maonekedwe ndi m’chikhalidwe (ife sitiri chinyezimiro mu chikhalidwe ndi mu maonekedwe Ake chifukwa tisiyana ndi Angelo omwe samachimwa!) cha Mulungu. Kotero tidziwe lero kuti Angelo sanayambanepo ndi Mulungu, ntchito yawo ndi kumvera ndi kuchita zonse mwa malamulo a Chiuta nthawi zonse.

ANGELO NDI OKHULUPIRIRA

Tikhulupirira kuti pangakhale chifukwa chokwanira kuti tiganize zoti munthu wokhulupirira mu choonadi aliyense amakhala ndi M’ngelo wake wake omuyang’anira m’moyo wake. Komanso akhoza kukhala Angelo ambiri oyang’anira munthu wachipembedzo m’modzi yemweyo. Tiyeni tiwerenge ndime ziri m’munsi’zi:

-“...*M’ngelo wa Mulungu azinga kuwatchinjiriza iwo akuopa Iye, Nawalanditsa iwo...*” (Masalmo 34:7).

-“...*tiana iti takukhulupirira ine (i.e. wochepa m’chikhulupiriro)*” (Zekariya 13:7 cp. Mateyu 26:31) ...*pakuti...angelo awo apenya chipenyere nkhope ya Atate wanga wa Kumwamba*” (Mateyu 18:6,10).

-Akhristu oyambirira anawonetseratu kuti adakhulupirira zoti Petro anali ndi M’ngelo womusamalira (Machitidwe 12:14,15). Leronso zikhoza kutheka kuti pakati pathu pamakhala a Ngelo omwe amatiyang’anira ndipo amaonanso zochita zathu za tsiku ndi tsiku koma mwina sitingathe kuzindikira ichi.

-Ana a Israeli anayenda podutsa Nyanja yofiira (Red Sea), motsogoleredwa ndi M’ngelo mu chipululu pa ulendo wao wopita ku dziko lawo la malonjezano. Kudutsa nyanja yofiira ndi chiphiphiritso cha “Ubatizo wamadzi” (1 Akorinto 10:1), kotero sicholakwika kuganiza kuti ifenso timathandizidwa ndi M’ngelo

mu moyo wathu paulendo wathu wachikhristu mu zipululu zosiyana siyana padziko lino lapansi kupita ku “Ufumu ulin’kudzawo”.

Monga tawona, tiri ndi mwayi waukulu pozindikira kuti Angelo ali ndi ntchito imodzi yokha ndiyo yotumikira Yehova; Koterotadziwa kuti Angelowo sachimwa; Ndipo atakhala kuti amachimwa, kukadakhala kobvuta kwambiri kuti apatsidwe udindo waukulu woyang’anira za okhulupirira mu chowonadi cha Mulungu ngati momwe tawerengera m’mwamba’mu. Kwaife ndi tsoka lalikulu ngati sitikhulupirira izi.

Taphunzira kuti Angelo mu uthunthu ndi makhalidwe awo:-

- Chake
- Ali ndi Umuyaya Wa Mulungu ndi thunthu mu chifanizo
 - Samachimwa
 - Amachita zonse pomvera malamulo a Mulungu
 - Ndinjira Yake Ya Yehova ndipo Mulungu amalankhula ndikuchita zonse kudzera mwa Angelo’wo (Masalmo 104:4)

KOMA.....?

Matcharitchi ambiri a chikhristu amakhulupirira kuti Angelo amachimwa ndipo kuti Angelo ochimwa akadalipo mpaka lero omwe amathandizanso kuti anthu azichimwa padziko lapansi. Tinenapo zambiri za mfundo yolakwika imene’yi mu Phunziro 6. Pakadali pano tiyeni tiwonere limodzi mfundo izi:-

-Zikhoza kutheka kuti ife tisanalengedwe kudalidi chilengedwe china choyamba monga timawerenga m’buku la Genesis1. Ndizodziwikiratu kuti Angelo onse omwe alipo lero amadziwa **“zabwino ndi zoyipa”** (Genesis 3:5) mwina, chifukwa choti anawona kale ndi kukhalapo mu umoyo omwe ife tiri nawo lero’wu. Zoti ena mwa olengedwa’wa anakhalapo nthawi yoyambayo ndipo kuti adachimwapo sitingakaniretu; chachikulu ndi choti zonsezi ndi nkambakamwa chabe zomwe malirime a anthu amakonda kungokamba ngati nthano. Ife tikudziwa kuti Baibulo limatiuza zinthu

zokha-zokhazo zomwe ife tiyenera kudziwa ndikuchita lero, zomwe tiyeneranso kudziwa kuti Angelo samachimwa; komanso kuti Angelo onse amamvera kwathunthu Yehova Mulungu Wathu. Izi zidaonekeratu pamene Angelo akhala akutumidwa kwa okhulupirira osiyana-siyana padziko.

-Sikungakhale Angelo kapena chilengedwe chomwe chinali cha uchimo kumwamba chifukwa timadziwa kuti tchimo linayamba m'munda wa Edeni osati kumwamba. Kumwamba komwe kumakhala Mulungu yemwe ali ***“Inu Wamaso Osalakwa, Osapenya, Osakhoza kupenyenera chobvuta, mupenyereranji iwo akuchita mochenjera, ndikukhala chete pamene woyipa a mmeza munthu wolungama woposa Iye Mwini”*** (Habakuku 1:13); Momwenso, Masalmo 5:4,5 akukananso chonchi: ***“..Pakuti Inu sindinu Mulungu wakukondwera nacho choyipa, mphulupulu sikhala ndi Inu, Opusa sadzakhazikika pamaso panu: Mudana nawo onse akuchita zopanda pake”***. Apa ife tiyenera kukaniratu zoti Mulungu angakhale ndi Angelo ochimwa m'mwamba; ndipo zoti kudali kuwukira Mulungu Kumwamba; komwe kunachitika ndi Angelo omwe ndi ochimwa chingakhale chinthu chosayenera kuti chikambidwe ndi munthu owerenga ndi kukhulupirira Mau eni eni a Mulungu ngati momwe mwadziwerengera pamwambapa. Mulungu Wamphamvu zochulukira akhoza kugonjetsa choyipa chiri chonse chomwe chingasokoneze chilengedwe chake. Choncho, tikachimwa sindiye kuti tachimwa chifukwa cha Satana yemwe angagonjetsedwe ndi Mulungu ayi, koma zilakolako zathu.

-Liwu la chiGreek lomasuliridwa kuti ***“Angelo”*** mu Baibulo ndilo kutanthauza kuti ***“Mtumiki”*** monga tanenera kale; Kotero, liwu limeneli lingagwiritsidwe ntchito potanthauzira ***“Mtumiki”*** yemwe ndi ***“M'ngelo”*** Wa Mulungu Wakumwamba kapenanso anthu omwenso amachimwa mu umunthu wao ngakhale ali ***“atumiki”***. Mwachitsanzo, tiri ndi atumiki mu mipingo mwathu mosiyana-siyana ngakhale atumiki athu samagwira ntchito yomwe ***“Mtumiki”*** Wa mu Baibulo ayenera kugwira.

-Maganizo oti Angelo ochimwa ndi ochita zoyipa alipo, ndi chikhulupiriro chosagwirizana ndi Baibulo kotero ndi chikunja.

Chimodzi modzinso chikhulupiriro chosangalala pa tsiku la Khrismasi sichisangalalo chogwirizana ndi Baibulo ayi. Palibe chilongosoko chirichonse chamtundu wotere mu Baibulo chifukwa tonse timadziwa kuti sizoonza kuti tsikuli ndi tsiku lomwe anabadwadi Yesu Khristu. Pali chisangalalo chomwe chinkachitika ku Rome nthawi yakale patsikuli ndipo anangolisandutsa tsikulo kuti likhale lokumbukira kubadwa kwa Yesu. Izi ndi zina zomwe zimapangitsa kuti Mau a Mulungu asokonekere chifukwa anthu ambiri amaphatikiza chikunja ndi Mau a mu Baibulo.

-Tikudziwa kuti pali ndime zina zomwe anthu ndi akhristu amatcharitchi ena amagwiritsa ntchito pofuna kutsimikiza kuti zomwe akuchita zigwirizane ndi momwe iwo akuganizira, monga zoti Angelo amachimwa. Pali kabuku kena komwe mutu wake ndi: ***“Kufunafuna Satana”*** ndipo mukhoza kuwerenga kabukuka mutayitanitsa ku adiresi iri komaliza kwa buku lino. Mavesi amenewo sakugwirizana ndi zomwe amakamba anthu amene amakhulupirira zinthu zotere kotero, ndizotsutsana kwambiri ndi chiphunzitso cheni cheni cha Buku Lopatulika. Mukhoza kuona nokha zomwe mwawerenga mu Phunziro lino kuti ndi zoonza zokha zokha posiyanyitsa ndi nkambakamwa zomwe timamva tsiku ndi tsiku mu mawailesi kapena nthawi zina mu mapepala. Chimene amafuna Mulungu ndi kuti ife tizionetsetsa chisamariro cha kasungidwe ka Mau ake omwe amayenera kukhala ngati mlozo wolozera kakhaliidwe kathu padziko lino lapansi. Ngati sitingathe kutsata chilongosoko cha Baibulo, ndiye kuti tasemphana ndi chifuniro cheni cheni cha Namalenga wathu’yo. Ziri kwaife kutsata kapena kukana chilongosokochi popeza Iye Mwini anatipatsa ufulu wosankha zomwe ife takonda kuti tichite, koma tizindikire mphotho yake ya masankho athuwo.

MPATUKO 1 : “MULUNGU NDI MZIMU” (Yohane 4:24)

M’phunziro 2, tifotokoza mwatsatane-tsatane zambiri zokhudza “Mzimu Wa Mulungu”. Mwachidule, tingati Phunziro 2 tiphunziramokuti kuti “Mzimu Wa Mulungu” ndi “Mphamvu Yake” kapenanso titi “Mpweya Wake” Wa

Mulungu ndipo kuti mzonsezi, maonekedwe ndi khalidwe lake la Mulungu zimaoneka mu Mzimu'wo ukagwira ntchito yake yapamwamba. N'chifukwa chake, pa Yohane 4:24 timawerenga kuti "Mulungu ndi Mzimu" ndipo ndi kofunika kuti kumasulira kwa mau amene'wa kuzikhala koyenera (ma Baibulo a R.S.V. ndi N.I.V.), mwaichi Mzimu Wake umaonetsa ntchito ndi khalidwe lake.

Mulungu amadziwikanso mu ntchito zambiri ngati izi:

"Mulungu Wathu ndiye moto wonyeketsa" (A Hebri 12:29).

"Mulungu ndiye kuunika" (1 Yohane 1:5)

"Mulungu ndiye Chikondi" (1 Yohane 4:8)

"Mau" (mu chi Greek "Logos"—"ndondomeko," "cholinga," "Ganizo") ***ndiye anali Mulungu*** (Yohane 1:1)

Choncho, "Mulungu ndi chikhalidwe ndi zochita zake." Sichingakhale chanzeru kunena kuti chikondi cheni chenicho ndi Mulungu chifukwa chakuti timawerenga kuti "Mulungu ndiye chikondi" ayi. Apa tikufuna kunena kuti, "Mulungu ndiye chikondi" n'kufotokozera khalidwe limodzi la Mulungu ndipo mau amene'wa, akutsimikizira zambiri za chikondi cha Mulungu pa omutumikira ake. Tikati uyu ndi "okoma mtima" sizitanthauza kuti ndi dzina lamunthuyo ayi koma kuti khalidwe lake ndi kukoma mtima kokha kokha, kuchita zabwino kwa anzake. Motero, kunena kuti Mulungu ndi Mzimu (Yohane 4:24) sizitanthauza kuti alibe thupi ndipo kuti ndi Mzimu woyenda yenda wokha wopanda maso, manja ndi zina, monga ena amanenera ayi. Tikatero, ndiye kuti tikukana kuti Mulungu alipo. Choti tidziwe apa ndi chakuti mbali imodzi ya chikhalidwe cha Mulungu ndi Mzimu kutanthauza kuti ***"ndi Wamphamvu"*** kapena kuti ***"ali ndimphamvu"***.

Mzimu ngati Mphamvu Ya Mulungu imatumizidwa ndi Mulungu Mwini kuti athe kuchita zinthu zosiyana siyana mogwirizana ndi cholinga komanso chikhalidwe cheni cheni cha uzimu. Timawerenga kuti mzimu (Mphamvu Yake) inalengedwa ndi Iye (Amosi 4:13). Mulungu amatha kupatula Mphamvu yake (Mzimu) kuti ikwaniritse ntchito zina mwapadera, zomwe

zikuonetsadi kuti pali kusiyana pakati pa Mzimu ndi Mulungu yemwe ali Mwini Wake Wamphamvu'yo.

Werengani zitsanzo ziri m'munsimu:

“...Iye amene anayika Mzimu Wake Woyera pakati pawo” (Yesaya 63:11)

“...Pa Iye ndidzayika Mzimu wanga,” (Mateyu 12:18)

“...Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera” (Luka 11:13)

“...Mzimu alikutsika kuchokera ku Mwamba monga nkunda (Yohane 1:32)

“...Ndidzathira cha Mzimu Wanga pathupi lirilonse” (Machitidwe 2:17).

Malo ambiri amene timawerenga mu Baibulo, tiona kuti pali kusiyana pakati pa Mulungu ndi Mzimu Wake (Mphamvu Yake). Ena ambiri mwa akhristu, amakhulupirira kuti pali milungu itatu yofanana ndipo kuti Mulungu ndi mu modzi mwa atatuwo. Iwo amanena kuti Mulungu ndi ofanana ndi Yesu komanso Mzimu Woyera. Izi zitakhala kuti ziri choncho, Yesu sakanabadwa ndiponso sakanakwaniritsa lonjezo kapena kuti “Mau anali kwa Mulungu ndipo Mau'wo ndi Mulungu,” (Yohane 1:1); omwe pachiyambipo Mulungu analonjeza zakutsogolo kuti Mwamphamvu Yake, mdzakazi adzabala mwana wamwamuna. Tiona apa kuti ulosi uwu analozera zakubadwa ndi ulaliki wa Uthenga Wabwino wa Yesu.

Pemphero lathu lingakhale loyenera ngati titadzera mwa Yesu popeza Iye ndi njira yathu kuti mau ndi zobvuta zathu zimveke kwa Mulungu. Koma ngati Mulungu'yo alibe maonekedwe eni eni monga momwe Yesu ankaonekera pamene anakwera kumwamba, ndikutinso amafanana mphamvu zake ndi milungu iwiri ija yomwe analenga ndi Iye yemwe, ndiye kuti pali bvuto lalikulu pakati pa anthu apadziko. N'chifukwa chake Buku Lopatulika limatikumbutsa za ubwino wake wopemphera kwa Mulungu kuti azitithandiza kumvetsa bwino Mau ake motero, tikazindikire maonekedwe ake eni eni ndi Uthunthu Wake weni weni Wakumwambako (Mlaliki 5:2; Mateyu 6:9; 5:16; 1 Mafumu 8:30), ndiponso kuti Yesu tsopano ali kudzanja lamanja la Mulungu

Atate (kutanthauza kuti Mulungu ali muthunthu wake wake ndipo alinso ndi dzanja) kulandira mapemphero athu ndi kupereka kwa Atatewo (1 Petro 3:21; a Hebri 9:24).

Onani kuti Yesu anakwera kumwamba ngati munthu mu uthunthu wa umunthu mwaichi, anapita kwa Mulungu yemwense ali mu uthunthu wotere ndipo ndi ofanana ndi maonekedwe ake. Sizikanatheka kuti Yesu apite kumwamba mu maonekedwe osiyana ndi Mulungu amene akukhala naye mpaka lero. Tiyenera kudziwa apa kuti Mulungu ali ndi Mzimu (Mphamvu) ndinso kuti ali ndi maonekedwe eni eni monga anthu, Yesu ndi Angelo amaonekera. Kotero, tizipemphera kwa Mulungu wachikondi, wamphamvu komanso okonzeka kulandira pemphero'lo ndikutiyankha mu chikondi chake.

MPATUKO 2 : KUGWIRITSA NTCHITO DZINA LA MULUNGU

Taona kuti dzina la Mulungu ndi la Mwana Wake Yesu Khristu maina a matanthauzo. Tikamakamba za “Mulungu” ndiye kuti tikukhudza mfundo yofunikira zedi pa zakudabwitsa, cholinga, chikondi ndi choonadi chake. Sityenera kumangotchula dzina la Mulungu pachabe popeza tikhoza kudzitengera tsoka kwaife tokha. Motero, yense ofuna kuchita chifuniro chake, ofuna kumulemekeza Iye, sadzatchula dzina lake pachabe. Tikudziwa tonse kuti chikhalidwe chathu chimasintha, chifukwa chotengera makhalidwe oyipa, auchimo amakono kotero, ife timafuna tipange zinthu zofanana ndi anthu otaya chipembedzo cheni cheni patsogolo. Munjira iyi, timanyoza Mulungu pokonda zinthu za mudziko chomwe chiri chinthu chosayenera kwaife ngati olakalaka kupeza chipulumutso. Tiyeni tizipemphera kwambiri kwa Mulungu kotero atithandize ndipo mwachikhulupiriro tidzathandizidwa. Tikatero, ngakhale onse amene ali pafupi ndi ife poona zochita zathu, adzakumbukira kuti kunyoza Mulungu ndi kulakwa ndipo ife tidzakhala ngati tawalalikira mu makhalidwe athu pakati pa anzathu'wo: “...*chifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosachimwa amene atchula Dzina Lakelo*” (Deuteronomo 5:11).

Ena amanena kuti pokha pokha munthu atatchula mayina awiri a chi Hebri a *Yahweh* kapena kuti *Yehova* (matchulidwe awiri a dzina limodzi lomwelo koma osiyana kamvekedwe) popemphera kwa Mulungu, sangapulumuke. Amene amakonda kunena zimenezi ndi a mpingo wa Mboni za Yehova.

Tinene pano kuti kutchula dzina kokha sikungapulmutse munthu. Tawona kuti tiyenera kumvetsa ndi kuzindikira matanthauzo osiyana siyana a Mau Oyera ndi kuchita chifuniro chake cha Mulungu, monga kubatizidwa ngati momwe Mau ake amatiuzira kuti ife tizichita ndipo tikatero, tidzapulumutsidwa.

Tinenenso kuti anthu omwe amalimbikira zimenezi, ndi amene akuthandiza kwambiri kuti anthu aziwona chipembedzo ngati kokapembedzerako mizimu komwe mayina ndiwo amatenga mbali yaikulu, komanso amanyoza anthu ena chifukwa cha katchulidwe ka mayina'wo. Izi ndi zopanda ntchito. Tinene mwaichi, kuti kutchula dzina la Yahweh kapena Yehova mpemphero sizisiyana ndi kutchula dzina la Mulungu, Namalenga, Chiuta, Chisumphi, Mphambe, ndi maina ena otero popeza zonsezo zikuyimira Mulungu Yemwe'yo koposa m'chilungamo. Taphunzira kale kuti Mulungu ali ndi maina ambiri.

Onse obatisidwa mwandondomeko yake ayenera kudziwa ndikukhala ndi chiyembekezo champhamvu Yake ngakhale angagwiritse ntchito maina a Mulungu osiyana chachikulu ndi kuzindikira chimene chiyenera kuchitika pamene apembedza Mulungu. Chipangano Chatsopano chimagwiritsa ntchito maina a Mulungu ambiri osiyana ndi a mu Chipangano Chakale; izi sizitanthauza kuti owerenga Chipangano Chatsopanochi sangapulumuke ayi. Baibulo silikambapo kalikonse za dzina kapena maina oyenera kutchulidwa ndi anthu ambiri pa chipembedzo chathu kwa Chiuta. Petro akukamba za okhulupirira ngati; *“mkhristu”* osati wa *“mboni Ya Yehova kapena Yahweh”* ayi (1 Petro 4:6) choncho, kaya ena amati Chiuta kapena Namalenga zilibe kanthu chachikulu ulemu upite kwa Iye Mulungu.

Tikalimbikira kugwiritsa ntchito mau oti “Yehova” kapena “Yahweh” kuti ndi okhawa oyenera kutchulidwa, ndiye kuti tikupembedza maina osati Mulungu. Koteru sitingathe kuona kufunika, mbali ndi gawo la Yesu Khristu pa chipulumutso. Ena amakonda kuti pa pemphero lililonse ngakhale mkulalikira kumene, ayenera kutchula kapena kutamanda dzina la Yesu lokha pofuna kusiyantsa ndi kufunikira kwa Mulungu Mwini. Timayenera kuwerenga Baibulo mofatsa kuti tizindikire mbali zonse zomwe Yesu Khristu ndi Mulungu amatenga pa chipulumutso chathu tiri m'moyo uno.

Akhristu oyambirira kalelo, ankadzitchula maina osiyana-siyana pomwense sanayikepo dzina la Yehova ngati m'ndime zotsatirazi:

“...mbumba ya Israeli ...” (Aefeso 2:12)

“...mpingo wa obadwa oyamba olembedwa m’mwamba.....” (A Hebra 12:23).

“..Eklezia wa Mulungu wogulidwa ndi mwazi” (Machitidwe 20:28).
“...Eklezia wa Mulungu wamoyo, mzati ndi m’chirikizo wa choonadi..” (1 Timoteo 3:15).

“....Nyumba Ya Mulungu.....” (1 Timoteo 3:15)

Timachita chidwi kuona kuti okhulupirira oyamba aja sankadzitchula kuti anali “Akhristu” dzina lomwe linali lonyozeka pakati pa anthu panthawi’yo kotero anthuwo ankaphedwa chifukwa chodzitchula mkhristu. Ngakhale zinali choncho, iwo analimbikabe kuchita chifuniro cha Mulungu modzipereka pozindikira kuti munthu sapeza chipulumutso chifukwa chodzitchula maina.

MPATUKO 3 : MULUNGU ADZIWONETSA KWA ANTHU

Maphunziro otsatira’wa ndiobvuta kuwamvetsetsa kotero ndi kofunika kuyikapo mtima ndipo tikatero, tidzapindula komanso tidzaona tokha kufunikira kwake kowerenga ndikudziwa zinthu za mtengo wapatali ngati zimenezi. Mbali yamaphunziro amene’wa tawaphatikiza mu phunziro lino ndi cholinga choti muzindikire bwino zambiri ya Mulungu ngati m’mene Baibulo limanenera osati monga buku lino kapena anthu amafotokozera mu mipingo kapena paliponse ayi.

Mulungu amasankha yekha mtumiki wake kuti dzina lake likawululidwe ndikutinso limveke kulikonse komwe Iye Mwini afuna. Choncho, atha kutuma anthu ndi Angelo ngakhaleenso Yesu, pofuna kukwaniritsa kumveketsa dzina lake. Iyi ndi mfundo imodzi yomwe imatithandiza kumveketsa dzina lake powerenga Baibulo. Tikawerenga Baibulo mu chiyero ndi mchoonadi, tidzanthunthumira Mau ake. Mwana aliyense amatchukitsa dzina la makolo ake maka maka akamachita zabwino, bambo wake amasangalala naye. Izi

zimaonetsa kuti mwana'yo ali ndi ntchito zabwino zambiri zofanana ndi makolo akewo mu chikhalidwe ngakhale ndi mu maonekedwe omwe. Nthawi zina amagwiritsa ntchito maina onse a bambo wake poyika "Junior" komalizira kwa mainawo. Izi zitionetseratu kuti mwanayo sangakhale chimodzi-modzi ndi bambo wake aja ngakhale kuti amafanana kwambiri ndi bambo'wo m'maonekedwe kuphatikizapo maina. Munthu aliyense woyimira malo antchito (kampani) amalankhula m'malo mwa onse ku kampaniko; Akayika telefoni amatchulanso dzina la kampaniyo, osati dzina la munthu oyankha uja chifukwa chakuti amagwira ntchito ku kampaniyo ayi. Yesu ndi atumiki ena a Mulungu, analalikirira Uthenga Wabwino pofuna kuwonetsa ubwino ndi kumveketsa dzina la Mulungu. Ntchito zawo zinabukitsa Dzina la Mulungu kudziwika paliponse popeza iwo ngati ana a Mulungu, anachita zabwino pakati pa anthu momvera kholo lawo lalikulu la muyaya.

ANGELO ONYAMULA DZINA LA MULUNGU

Timawerenga pa Eksodo 23:20,21 pamene Mulungu anawuza ana a Israeli kuti M'ngelo adzawatsogolera paulendo wao; "...*dzina langa liri mwaine*". Dzina lake la Mulungu ndi "*Yahweh*" kapena "*Ambuye*"; ndipo akanakhala kuti amalankhulayo ndi M'ngelo, dzinali limakhala mu malembo ang'ono mu Baibulo (onani kumasulira m'Baibulo la N.I.V. ndi A.V.). Timawerenganso pa Eksodo 33:20 kuti palibe munthu yemwe angawone nkhope ya Mulungu nakhalabe ndi moyo; koma pa Eksodo 33:11 tiwerenganso kuti; "*Ambuye (Yahweh) ananena ndi Mose mopenyana maso ndi maso monga munthu alankhula ndi bwenzi lake*" mwachitsanzo, momasuka ndi mwachikondi. Zikhoza kutheka kuti sanali Mulungu yemwe analankhula maso ndi maso ndi Mose pa nthawi'yo chifukwa tawuzidwa kuti palibe angawone Mulungu nakhalabe ndi moyo. Timamva kuti anali M'ngelo yemwe anamvala dzina la Mulungu koteru, Yehova analankhula maso ndi maso ndi Mose ngakhale anali M'ngelo yemwe analankhulayo (Machitidwe 7:30-33).

ANTHU NDI DZINA LA MULUNGU

Ife tikafuna kumvetsa bwino, tiyenera kuwerenga mofatsa Yohane 10:34-36. Tiona kuti a Yuda apa ankalakwitsa ngati momwe akhristu ambiri lero amachitira. Iwo ankaganiza kuti Yesu ananena kuti Iye ndi Mulungu. Pofuna kukonza maganizo olakwika otere, Yesu anati; "*Kodi sikunalembedwe m'chilamulo chanu, Ndinati Ine, muli milungu? Ngati anatchula milungu*

iwo amene Mau a Mulungu anawadzera...kodi inu munena za Iye, amene Atate anampatula namutuma kudziko lapansi, 'uchita mwano' chifukwa ndinati, Ndiri Mwana wa Mulungu?" Yesu apa ankawakumbutsa kuti mu Chipangano Chakale kunalembedwa kuti anthu anawuzidwa zoti iwo ndi milungu. Mau amene anawakumbutsa Yesu anali ochokera pa Masalmo 82 pomwe tiwerenga za oweruza a ana a Israeli kuti anatchulidwa milungu ndi Mulungu.

Monga taphunzira kale, dzina leni leni la Mulungu ndi *"Yahweh Elohimu"* kutanthawuzira kwake ndiko *"Ndidzabvumbuluka m'khamu la amphamvu ambiri"*. Tikhoza kunenanso kuti okhulupirira eni eni angakhale amodzi wa *"amphamvu ambiri amene'wa"*, ndipo kuti adzakhaladi amodzi eni eni mu masiku akudzawa mu Ufumu wake. Tiwerenge Yesaya 64:4 ndinso 1 Akorinto 2:9, ndipo tiona kuti zonse zakambidwazi zidzakhala choncho. *"...Anthu sanamve ndikuzindikira m'makutu mwawo, komanso sanamve Mulungu wawo, zomwe inu munakonzera anthu anu omwe akudikira kubwera kwa Iye."* Paulo naye akutikumbutsanso za Mau omwe'wo pamene ananena pa 1 Akorinto 2:9-10: *"Koma monga kulembedwa,...zimene diso silinaona, ndi khutu silinamva, Nizisinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zonse Mulungu anakonzera za iwo akumukonda Iye. Koma kwa ife Mulungu anationetsera izi mwa Mzimu Wake."* Yesaya 64 akunenanso kuti kupatula Mulungu, palibe angamvetse zomwe Iye Mwini anawakonzera omwe amakhulupirira; pamene 1 Akorinto 2:10 akunena kuti zinthu zimenezi zinawululidwa kwaife kotero m'njira imeneyi, ife ndife Mulungu: osati Mulungu weni weni ayi koma chiphiphiritso ndi chifanifani cha Mulungu kudzera mu chikhulupiriro ndi ubatizo mdzina lake tikadziwa choonadi. Tikhozanso kunena kuti ndife nthambi imodzi ya "amphamvu ambiri" Mphukira ya tsinde lake la chikhristu lero pakati pa amitundu.

YESU NDI DZINA LA MULUNGU

Tafika ndi kuzindikira tsopano kuti Yesu ngati Mwana Wa Mulungu komanso chiwonetsero cha Mulungu pakati pa anthu, ayenera kukhala ndi dzina la Mulungu. Ananenapo kuti, *"Ndadza Ine m'dzina la Atate anga"* (Yohane 5:43). Chifukwa choti Yesu anamvera, anakwera kumwamba ndipo Mulungu, *"...anakwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse"* (Afilipi 2:9). Kotero, timawerenganso kuti Yesu akunena, *"...ndipo ndidzalembe pa iye (wokhulupirira) dzina la Mulungu Wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu"*

wanga, la Yerusalemu Watsopano...ndi dzina langa latsopano” (Chibvumbulutso 3:12). Patsiku la chiweruzo, Yesu adzatipatsa dzina la Mulungu; Koteru, ndiye kuti tidzakwaniritsa kunyamula kapena kubvala dzina la Mulungu kwathunthu komanso kokwanira. Dzina limeneli *akulitchula “Dzina langa latsopano”* Tikumbukire kuti Yesu analemba Buku la Chibvumbulutso (kudzera mwa Yohane) zaka zingapo zitadutsa atakwera kale kumwamba komanso atapatsidwa kale dzina la Mulungu monga tawerenga pa Afilipi 2:9. Choncho, atha kutchula Dzina la Mulungu, “Dzina langa latsopano” lomwe Iye wangopatsidwa kumene panthawiyo. Zikatero, ndiye kuti tsopano timvetsa bwino zomwe Yesaya 9:6 ananena zokhudza Yesu kuti *“...adzamutcha* (onani pamenepa) *Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga Wamtendere...”*. Ulosi uwu ndi umene timawerenga kuti Yesu ananyamula maina onse a Mulungu, koteru akwaniritse kubvumbulutsa, kutchukitsa ndi kumveketsa dzina lake la Mulungu. Chifukwa chaichi, anatchulidwa *“Emanueli”* kutanthauza kuti “Mulungu ali nafe” ngakhale Iyeyo sanali Mulungu Mwini weni weniyo.

Munthu aliyense sayenera kukhala ndi milungu iwiri kapena kuti sayenera kuphatikiza chipembedzo ndi chikunja. Kutsata zinthu zimene siziri zogwirizana ndi Mau ake a Mulungu, kenaka, ndi kutengako timau pang’ono mu Baibulo pofuna kupanga chipembedzo china chosiyana ndi chipembedzo cha mu Buku Lopatulika, ndi kulakwitsa kwambiri chifukwa ndi sizimagwirizana ndi chifuniro cha Mwini wake Mlengi. M’njira iyi, chikhalidwe, maonekedwe, ndondomeko ndi zofuna za Mulungu sitingazidziwe pokha pokhapo titasintho maganizo athu ndikutsamira pa zolembedwa mu Baibulo. Timayenera kuzindikira kwathunthu kuti Mau a Mulungu samapita pachabe motero, ngati ndi koyenera kudziwa dzina ndi cholinga chake, tiyenera kulidziwitsitsa dzinalo ndipo tikalidziwa, tidzachita zonse mu chifuniro chake koteru kuti tidzapindula mu kulandira moyo wosatha. Kodi ife tingapulumsidwe bwanji ngati sitidziwa dzina la Ambuye wathu kwathunthu?

PHUNZIRO 1: MAFUNSO

1. N'chiyani chimene chingathandize kukulitsa ndi kukhwimitsa chikhulupiriro chathu mwa Mulungu?
 - (a) Kupita ku tcharitchi
 - (b) Kuphunzira za M'Baibulo ndi kupemphera
 - (c) Kumalankhulana ndi akhristu anzathu
 - (d) Poona kwambiri zachilengedwe
2. Ndi ziti mwa ziganizo ziri m'munsizi zomwe zikufotokozera bwino za Mulungu kuti ndi ndani?
 - (a) Kungokhala ndi maganizo ake m'mitima mwathu
 - (b) Ndi mzimu umodzi wokha womwe umakhala mlengalenga
 - (c) Kulibe Mulungu
 - (d) Ali ndi makhalidwe eni-eni, mu uthunthu la umunthu ndi maonekedwe a umunthu.
3. Kodi Mulungu ndi
 - (a) M'modzi mu umodzi?
 - (b) M'modzi mwa Atatuwo?
 - (c) Milungu yambiri mu umodziwo?
 - (d) N'kosatheka kufotokozera m'njira iriyonse?
4. Kodi Dzina la Mulungu loti "Yahweh Eloimu" limatanthauzani?
 - (a) Iye yemwe Adzakhale
 - (b) Iye Amene Adzabvumbuluke m'khamu la Amphamvu ambiri
 - (c) Wamkulukulu m'modzi
 - (d) Mphamvu
5. Kodi liwu loti M'ngelo limatanthawuzani?
 - (a) Wokhala ngati munthu
 - (b) Wokutidwa ndi mapiko
 - (c) Mtumiki
 - (d) Wothandizira Mulungu
6. Kodi Angelo akhoza kuchimwa?
7. N'chiyani chimene chimakupangitsani kukhulupirira kuti kudziko kuno kuli Mulungu?

Mukayankha chonde tumizani mayankho anu ku imodzi mwa ma adiresi alembedwa komaliza kwa buku lino:

PHUNZIRO 2

MZIMU WA MULUNGU

2.1 MZIMU WA MULUNGU - TANTHAWUZO

Monga tawerenga kuti Mulungu ali ndi thunthu leni-leni la umunthu, ndipo kuti amamva komanso kuti amatiwuzwa zofuna ndi zokonda zake ife ana ake, kuti akachite nafe m'miyoyo yathu mogwirizana ndi chikhalidwe chake. Mulungu amachita komanso kukwaniritsa zonse mwa Mzimu Wake. Ngati tifuna kudziwa Mulungu komanso kukhala ndi ubale wapadera ndi Iye nthawi zonse, tiyenera kudziwa zambiri ndikuzindikira ntchito yake ya “Mzimu wa Mulungu” mozama.

Tikudziwa kuti n’kobvuta kutanthawuzira mwachimvekere liwu loti “mzimu” (spirit). Tikakhala pa chisangalalo ndi anzathu, timati lero kwagwa mzimu wabwino. Zinthu zikatero, zimasonyeza kuti zonse zochitika pa chisangalalocho ziri m’malo mwake ndikuti zikuyenda bwino komanso mwandondomeko, m’chikondi ndi mogwirizana. Momwemo, Mzimu Wa Mulungu, umakamba ndi kufotokoza zambiri za Iye Mwini. M’chi Hebri, monga analemba Chipangano Chakale, “Mzimu (Spirit)” ndikutanthawuzwa kuti “Mpweya” kapena kuti “Mphamvu”; Motero, Mzimu Wa Mulungu ndiye kuti “Mpweya Wake”, zomwense zimaonetsa ndi kunyezimira maganizo ake. Tiwonanso kuti “mzimu” ndi liwu lomwe lingathanhawuzirensa maganizo kapena ntchito zake za mphamvu Mphunziro 4.3. Ili ndi liwu lomwe likuyimira ntchito zambiri mwa Mulungu monga tanena kale pamwambapa; mwachitsanzo, *“Mphamvu ya Mzimu Wa Mulungu”* (Aroma 15:19).

Sichinthu chachilendo kuwerenga m’Baibulo kuti maganizo a munthu amawonekera ndi ntchito zake, malankhulidwe ndi chikhalidwe chake (Miyambo 23:7; Mateyu 12:34). Tikawunika zonse zomwe timachita ife tsiku ndi tsiku, titsimikizira kwambiri zoonza zeni-zeni za mfundo imeneyi. Tikangoganizira za chinthu china, timayesetsa kuchipanga mwamaganizo athu. Mzimu wathu kapena kuti maganizo athu amatha kutilozera kuti tsopano tili ndi njala ndipo zikatero, timayesetsa kupeza chakudya nthawi yomwe tamva njala’yo. Titha kuwona nthochi ndipo chifukwa chakuti tayiona nthochi ija, maganizo amatifikira oti tidye osati chifukwa chakuti takhala tikuyifuna nthochi ija ayi, koma popeza tayiwona. Zitsanzo zaperekedwazi zingatiwonetse kutanthawuzwa kwa mau amene’wa a “mzimu” m’chilankhulo cha chi Hebri. Choncho, liwu loti “mzimu” m’chi Hebri, limatanthawuzanso kuti “Mpweya kapena maganizo” ndinso “Mphamvu”. Mzimu wathu (our

spirit) umaonetsa ife monga tirili m'maganizo choncho, ntchito zathunso ndi zotsatira zake za maganizo ndi mphamvu zathu. Ichi ndichitsanzo chabwino cha momwe Mzimu Wa Mulungu uliri; ndimphamvu zake zomwe Iye Amawonetsera Ukulu ndi ntchito zake pokwaniritsa zolinga zake ndi dziko lino lapansi. Tiona mwaichi, kuti Mulungu amaganiza kenaka n'kuchita chinthu chimene waganizacho, *"...monga ndaganiza, chotero chidzachitidwa; ndipo monga ndapanga uphungu, chotero chidzakhala"* (Yesaya 14:24).

MPHAMVU YA MULUNGU

Manunsu ambiri m'Baibulo, amaonetseratu kuti Mzimu Wa Mulungu ndiye mphamvu Yake. N'chifukwa chake pamene Mulungu anakalenga dziko lonse lino, *"...Mzimu Wa Mulungu unkayenda pamwamba pa madzi onse...Ndipo Mulungu anati, kuyere: ndipo kunayera"* (Genesis 1:2,3[translation]).

Mzimu Wa Mulungu, ndiye mphamvu zake zomwe Iye analengera zinthu zonse monga kuwala, mdima ndi zina zotero. *"Mwa Mzimu Wake ananyezimitsa (anakongoletsa) thambo; Dzanja lake linapanga njoka yochenjera"* (Yobu 26:13). *"Zakumwamba zinalengedwa ndi Mau A Yehova; Ndipo ndi Mpweya Wa Mkamwa Mwake khamu lawo lonse"* Masalmo 33:6). Choncho, Mzimu Wa Mulungu ndi:-

Mpweya Wake

Mau Ake

Dzanja Lake

M'njira izi, Mulungu amakwaniritsa zinthu zonse. Kotero, okhulupirira wonse ndiwobadwanso mwatsopano pomvera ndi kuchita chifuniro chake (Yohane 1:13), mwa Mzimu Wake (Yohane 3:3-5). Chifuniro chikuchitikadi mwa Mzimu Wake. *"Mukangotumiza Mzimu Wanu, zilengedwa; ndipo Mukonzanso nkhope ya Dziko lapansi,"* Masalmo 104:30). Mzimu'wu (Mphamvuyi) ndinjira yokhayo yokwaniritsa zinthu zonse zofunikira komanso ndinjira yomwe Mulungu anakwaniritsa chilengedwe chonse. Ngakhale zinthu zambiri zikuchitika padziko, zina zabwino ndiponso zoyipa, Mphamvu yake Ya Mulungu imathandiza m'chilengedwe cha zonsezi. Pona kuti Yesu

adanzunzika pamtanda, m'neneri wina adafotokozeratu kuti, **“Akasonkhanitsa mzimu wake (mphamvu yake) ndi mpweya wake; zamoyo zonse zidzatsirizika, ndi munthu adzabwerera ku mpfumbi”** (Yobu 34: 14,15). Mwanjira imeneyi, pofuna kudzipulumutsa m'mabvuto otere, Davide adapempha Mulungu kuti azimuthangata ndi Mzimu Wake (mphamvu yake) nthawi zonse chitsanzo, kusunga ndi kuteteza moyo wake (Masalmo 51:12).

Monganso tanena kale, tikafika Phunziro 4.3 tiona kuti mzimu womwe tinapatsidwa kuphatikizapo chilengedwe chonse, ndizinthu zomwe zimasunga ndi kuteteza moyo wathu. Tiri ndi **“mpweya wa mzimu wamoyo ”** mwa ife (Genesis 7:22), womwe unapatsidwa kwaife ndi Mulungu Yehova kuyambira patsiku lomwe tinabadwa (Masalmo 104:30; Genesis 2:7). Izi ndi zomwe zimupanga Iye kukhala **“...Yehova Mulungu Wa Mizimu ya anthu onse”** (Numenti 27: 16 cp A Heberi 12:9). Choncho, popeza Mulungu ndi msungi komanso mwini weni-weni wa miyoyo yonse ndi chilengedwe chonse, Mzimu Wake uliponseponse. Davide anazindikira kuti Mzimu Wa Mulungu umapezekaponseponse ngakhale pafupi ndi Iye komanso konse kumene angapite. Ndipo mwa Mzimu (mphamvu) umenewu, Iye ankadziwa zonse zomwe Davide anali kuganiza. Kotero, Mzimu Wa Mulungu ndinjira imodzi yomwe Iye amapezekerapakati pathu ngakhale Yehova akhala kumwamba.

“...Inu mudziwa kukhala kwanga ndi kuuka kwanga, Muzindikira lingaliro langa muli kutali... Ndidzapita kuti kuzembera Mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kezembera nkhope yanu?...Ndikukhala ku malekezere a nyanja (kuthawira kutali); kungakhale komweko dzanja lanu (mwachitsanzo, mwa Mzimu Wake/Mphamvu Yake) lidzandigwira” (Masalmo 139:2,7,9,10).

Mukamvetseta bwino bwino nkhani yonseyi, mukhoza kuona kuti Mulungu kwaife ndi Wamphamvu zopanda malire komanso zangwiro. Anthu ambiri ali ndi chikhulupiriro mwa Yehova ngakhale chikhulupiriro chawo chimakhala chopewera maka chifukwa chakuti samadziwa zambiri za Yehovayo; samamudziwa kweni-kweni popeza alibe luntha lowerenga mwachifatse kuti azindikire zambiri za dzina la Yehova.

Tikazindikira kuti Namalenga amakhala pafupi ndi ife mu umunthu komanso mwa Mzimu Wake yomwe iri Mphamvu Yake, moyo wathu udzasintha kwathunthu chifukwa tidzalola, kuyamika komanso kukhutitsidwa kuti

Ambuye Wathu Wamphamvuyo alipodi pakati pathu nthawi zonse. Tiri okutidwa ndi Mzimu Wake, womwe umatichitira umboni kudzera m'ntchito zake zomwenso zimaonetsa Umulungu pakati pathu. Tikhoza kuzindikira kuti ngakhale Davide analimbikitsidwa ndi maganizo a mtundu wotere: **“...Kudziwa ichi kundilaka ndi kundidabwitsa; n'chapatali ndipo sinditha kufikirapo...”** (Masalmo 139:6). Udindo wa munthu apa tiona kuti umabwera kwa munthuyo chifukwa chozindikira Mphamvu yeni yeni ya Mulungu. Tiyeni kotero, tilole komanso timvetse kuti Mau otere ndi Mau achilimbitso chokwanira pa moyo wathu. Maganizo ndi ntchito zathu zikhale zochita chifuniro chake. Pamene tikuyesayesa kuganizira za chikhristu chathu ndi ubale wathu ndi Iye, maka-maka ngati tikuyembekezera kubatizidwa, tidziwe kuti zimene zakambidwa apa ndi gawo lofunikira zedi m'moyo wathu wa chiyero. M'Mau ake a Mulungu kwa Yeremiya, akunenanso kwa ife lero: **“...Kodi munthu angathe kubisala kuti mobisika kuti ndisamuone iye? Ati Yehova. Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? Ati Yehova”** (Yeremiya 23:24).

MZIMU WOYERA

Taona m'Phunziro lapitali za Mzimu Wa Mulungu kuti ndi mutu waukulu komanso obvuta kuwumvetsa ngati sitingafatse nawo posanthula M'Buku Lopatulika. Tiyenera kuchita izi m'mphamvu ya chiganizo chake ndi mphamvu ya chikhalidwe mophatikiza maonekedwe ake m'chiyero; Mwaichi, amayendetsa zinthu zonse m'maganizo otere'wa. **“Monga munthu asinkha-sinkha mumtima mwake, Iyenso ali otero”** (Miyambo 23:7) choteronso, Mulungu weni-weniyo ndimagano ake ndipo ali mu Mzimu Wake (Yohane 4:24). Izi sizitanthawuza kuti Mulungu alibe uthunthu ayi (onani Mpatuko Oyamba). Kotero, kuti tizindikire kufunika ndi kukula kwa mutu umenewu wa “Mzimu Wa Mulungu”, nthawi zina tiyenera kuwerenganso za “Mzimu Woyera”. Mau oti “Mzimu Woyera” amapezeka mwapadera kawiri-kawiri m'Chipangano Chatsopano. Baibulo la Chingerezi la “Authorised Version”, mau amene amagwiritsidwa ntchito ndi “Holy Ghost” m'malo mwa “Holy Spirit”. Matanthawuzo a mau amene'wa anayenera kukhala “Mzimu Wa Mulungu” kapena kuti “Mzimu Wa Ambuye”. Izi zimaonekera pamene munthu awerenga Machitidwe A Mtumwi 2, pomwe kufotokozera zodzozedwa kwa atumwi ndi Mzimu Woyera nthawi ya Pentekositi, kwalembedwa mwa chindunji. Petro anawulula kuti ichi chinali chikwaniritso cha uloji wa Yoweri yemwe ananeneratu zodzozedwa kwa **“...Mzimu wanga”**

(wa Mulungu) (Machitidwe 2:17). Kuwonjezera apa, Luka 4:1 akunena kuti Yesu **“modzazidwa ndi Mzimu Woyera”** anabwerera kuchokera ku Yordano; kenaka m'nunsu yomweyo, Yesu analongosola kuti uku kunali kukwaniritsa Yesaya 61: **“...Mzimu Wa Ambuye Yehova uli paine;”** M'malo onsewa, Mzimu Woyera ukugwira ntchito chimodzimidzi ngati liwu la mu Chipangano Chakale la **“Mzimu Wa Mulungu”**.

Onaninso ndime zotsatirazi zomwe zikuonetseratu kuti Mzimu Woyera ndi **“Mzimu Wa Mulungu”** koteronso kuti zonsezi ndi ***Mphamvu ya Mulungu***:

“...Mzimu Woyera udzafika pa iwe (Mariya) ndi Mphamvu ya Wamkulukulu wa kumwamba idzakuphimba iwe” (Luka 1:35).

“...Mphamvu ya Mzimu Woyera...mu mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa mu mphamvu ya Mzimu wa Mulungu” (Aroma 15:13,19).

“...Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, ...koma unadza mu Mzimu Woyera” (1 Atesalonika 1:5).

Malonjezano a Mzimu Woyera kwa akuphunzira ake a Yesu ananenedwa ngati **“mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba”** (Luka 24:49).

Yesu mwayekha ananena **“...kuti Mulungu anamdzoza Iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu...”** (Machitidwe 10:38).

Ulaliki wa Paulo unkatchinjirizidwa ndi mphamvu yowonekeratu ya Mulungu: **“...Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga...koma anakhala m'chionetsero cha Mzimu ndi Mphamvu”** (1 Akorinto 2:4).

2.2 MAUZIRIDWE (MAPATSIDWE A MAU NDI MULUNGU)

Tafotokoza kuti Mzimu wa Mulungu ndiye mphamvu yake, maganizo ndi maonekedwe kapena chithunzi thunzi chake zomwe zimaoneka mu ntchito yomwe Mzimu Wakewo ukuchita pakati pathu. Tanena kale momwe Mzimu wa Mulungu unathandizira pa chilengedwe cha dziko lonse ndi zinthu zonse: **“Mwa Mzimu wake anyezimiritsa kumwamba”** (Yobu 26:13). Chilengedwe chinachitika ndi Mzimu wa Mulungu womwe unkayenda pamwamba pa madzi onse (Genesis 1:2). Pamene timawerenganso kuti **“...Ndi Mau a Mulungu Yehova”** dziko lonse linalengedwa (Masalmo 33:6), kotero, uwu ukhala ngati umboni waukulu kutsimikizira zomwe zinalembedwa mu Buku la Genesis pongonena kuti “Mulungu anati” zonse zinalengedwa. Chinanso ndi chitsimikizo kwaife kuti zomwe zinawuziridwa zikukwaniritsidwa pakati pathu mpaka lero. Ichi chikutsimikiziranso kuti Mzimu wa Mulungu umaonekera kwambiri m’maganozi ndi zofuna za Mulungu, ngati momwe zokamba zathu za tsiku ndi tsiku zimawonetsera chikhalidwe chatu ndinso zokonda zathu. Umboni wina timawupeza mwa Khristu Yesu pamene analongosola za izi kuti **“...pakuti mkamwa mungolankhula monga mwakusefukira kwake kwa mtima (maganizo)”** (Mateyu 12:34). Motero, ngati tilankhula zamumtima (maganizo) mwathu, tikuonetsa chikhalidwe chatu cha tsiku ndi tsiku koteronso, tikafune kudziletsa m’malankhulidwe oyipa, inde ngakhale podziletsa m’maganozi athu oyipawo. Mwaichi, tingati Mau a Mulungu ndi chithunzi-thunzi cha Mzimu Wake omwense ndi maganozi ake. N’chosangalatsa komanso madalitso amphamvu kuona kuti m’Baibulo muli Mau ake olembedwa ncholinga chakuti ife tidziwe zambiri za Mzimu wake kapenanso tinene kuti maganozi ake. Mulungu anakonza zonsezi powuzira mpweya wake wa Mau mwa aneneri ake. Ndipo ntchito imodzi yokhayo yofunikira yomwe inagwiridwa ndi Mzimu wake ndiyo kulemba Buku Lopatulika mosaphonyetsa koma mwa uthunthu wonse ndi chitsimikizo chokwanira.

KUWUZIRIDWA

Mulungu poyamba anali ndi Mau ndipo anawuzira mauwo mwa aneneri ake omwe analemba mu Buku Lopatulika molongosoka choncho, chifukwa

chaichi, timakhulupirira kuti Baibulo linalembedwa ndi Yehova. Aneneri anakhala ngati njira yoululira maganizo ake omwe adawasunga kwa kanthawi. Mauwa anali Mzimu wake kapena kuti maganizo ake kotero kuti zofuna zake lero timazidziwa powerenga m' mau ake. Paulo anamulimbikitsa Timoteo kuti azolowere ndikukhala pafupi ndi Mulungu m' mau ake, poganizira kuti ndimau a Mzimu wa Mulungu. Iye amatipatsa ndi kukwaniritsa zofuna zathu zonse, ndipo kuti ndi kofunika kudziwa zambiri zoonza zake za Mulungu zomwe timawerenga mu Mau ake:-

“...ndikuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu. Lemba lirilonse adaliwuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino...” (2 Timoteo 3:15-17).

Ngati Mau owuziridwa'wa angatipatsa nzeru zonse monga tawerengera m'mwambamu, ndiye kuti Mau a Mulungu ndi Mau a choonadi ndi Mau eni eni a Mulungu ndipo tiyenera kutsamirapo. Koma kodi ife timakhumudwa ndi Mau a mtengo wapatali ngati amenewa chifukwa chakuti sakupereka mfundo yogwirizana ndi momwe anzathu kapena ife tikufunira? Kodi ndi zoonza kuti mau amenewa angatilondolere ku chipulumutso? Ndi anthu angati lero pakati pathu omwe angayime nachitira umboni kuti awa ndi Mau ake eni-eni a chipulumutso mopanda mantha m'malo motanganidwa ndi chipembedzo chabodza chopanda matanthauzo? Ngati kulandira Mau amenewa kungatipindulire ife kuti tipeze chipulumutso, palibenso chifukwa chokhalira ndi mphamvu zina zapadera koma kulimbika pa Mau akewo omwe ndi okwanira pa moyo wathu wachikhristu. Kufuna mphamvu zina zapadera kumaonetsa kusakhulupirira Mau ake kotero timatsutsana ndi ulaliki wa Paulo womwe ndi wodzozedwa ndi Mulunguyo. Tikangonyamula Baibulo mu manja mwathu, nkukhulupirira kuti tanyamula Mau a Mulungu chimaonetsa chikhulupiriro cha mtengo wapatali. Sianthu ambiri omwe amanyamula Baibulo ndi chikhulupiriro cheni cheni ayi; ambiri'fe tiri ndi Baibulo chifukwa cha chizolowezi chakuti tipeze chithandizo kwa akhristu anzathu pa nthawi ya mabvuto. Baibulo limayenera kutikonza ife eni kuti tikhale ndi chiyembekezo chabwino, cha moyo wosatha osati kutithandiza mu mabvuto a moyo uno ayi.

Ana a Israeli ankafunitsitsa kuti amve zomwe Mulungu afuna iwo achite mu chikhulupiriro, pamabvuto kaya pa mtendere.

Chimodzi modzinso ife lero tiyenera kutsata chitsanzo chimenechi:-

“...Pakuti kwaifenso walaligidwa Uthenga Wabwino, monganso kwa iwo (ana a Israeli mchipululu); koma iwo sanapindula nawo Mau omvekawo, popeza sanasanganizidwe ndi chikhulupiriro mwa iwo amene adawamva” (A Hebri 4:2).

M'malo mokhala ndi chikhulupiriro mu mphamvu ya Mulungu kudzera pa chitsimikizo cha Mau ake mu Baibulo, ife sitimakhala ndi chiyembekezo koma kukayikira kokha kokha. Tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro pa zinthu zosaoneka ndi maso monga kumafunikira m'chiyero chake. Tiyeni tilimbike kuwerenga Mau ake mosatsata chidule, tizindikire bwino kuti tidziwe chomwe tikukhulupirira mu moyo wathu wachikhristu motero tikalandiridwe pamaso pake mogwirizana ndi zimene tachita. Tionetsetse kuti ngati wina watilalikira, tifufuze mokwanira mu Baibulo lomwe ndi Mau ake ndipo kuti m'menemo tapezamo mpfundo zolaligidwazo kuti ndizoyenera pamaso pa Mulungu. Tikatero, tikhala nacho chikhulupiriro cheni cheni choyima pa Uthenga Wabwino woona ndipo tiwubvale Uthengawo ngakhale mkuzunzika kumene kuti tikakhwime potchinjiriza choonadi chimenechi. Timvere Yehova mu Mau ake, mkutero, moyo wathu udzakhudzidwa ndi Mzimu wa Mulungu komanso mu mitima mwathu mudzadzazidwa ndi chiyero chake. Tikhulupirire kuti titamvetsa ndondomeko yonse ya cholinga cha Yehova, tidzapindula kopambana. Anthu ambiri lero sitizindikira Mau Oyera mozama chifukwa sitimamvetsa bwino bwino kuti kodi koyambirira kwa moyo wathu wachikhristu, timayenera tichite chiyani kuti tifike pa mzere wobatizidwa ndikukhutira kuti takonzeka kukwaniritsa zofuna za Mulungu. Nthawi zina zimaoneka kuti sitimakhala ndi luntha lomvetsetsa bwino chilongosoko cha kubadwanso mwatsopano chotsamira pa Buku Lopatulika.

Posafuna kuzindikira Mau otere, omwe ndimphamvu ya Uzimu komanso Mau eni eni othyakuka a Mulungu, akhristu ambiri lero ndi osokonekera kotero, anafika pokayikira kuti Mau a mu Baibulo sangawapulmutse, ndikuti sionse mau amene ali mu Baibulo omwe ndi owuziridwa ndi Mulungu. Amafika poganiza kuti ati Mau ena mu Buku Loyerali ndi maganizo chabe a anthu akale komanso akadaulo ndi akachenjede a ku Israeli omwe analemba mbali yaikulu ya Baibulo. Ife tikuti abale nonse muyenera kudzipereka kwathunthu

mu Mau ake chifukwa ndiwo Mau eni-eni a Yehova ndipo ife tikukutsimikizirani ichi kuti Mau akewo sadzapita pa chabe. Tisasewere ndi Mulungu Mlengiyo. Petro akutsimikizira maganizo'wa motere:-

“...Ndipo tiri nawo mau a chinenero okhazikika koposa; amene muchita bwino powasamalira, monga nyali younikira m'malo a mdima, kufikira kukacha, nikauka nthanda pa mitima yanu; ndikudziwa ichi (chofunika kwambiri) poyamba, kuti palibe chinenero cha chilembo chitanthawuzidwa pachokha, pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu ogwidwa ndi Mzimu Oyera analankhula..”
(2 Petro 1:19-21). Tifuna tenene kuti ndi kofunikira kutsata ndi kuchita monga Baibulo limatiphunzitsira osati monga ife timaganizira ayi. Chikunja ndi chiphunzitso cha Baibulo ndi zinthu ziwiri zosiyana.

Chofunikira kwambiri kwaife ndi kukhulupirira kuti Baibulo ndi Mau owuziridwa ndi Mulungu. Mwaichi, ndi koyenera kukhulupirira kwamphamvu ndi kudzipereka pa ntchito yake yaikulu mu chilungamo.

OLEMBA BAIBULO

Chikhulupiriro chokwanira pa Mau ake owuziridwa ndi chofunika komanso choyenera; anthu omwe analemba Buku Lopatulika anali odzipereka mu chikhalidwe chawo chotsamira pa malonjezo a Mulungu kotero mu chikhulupiriro, anawuziridwa ndi Mzimu Oyera womwe unawauzira polemba Buku Loyalali. Ndipo ngakhale analankhula kapena kulemba, sanali mau awo ayi koma ochokera kwa Mulungu. Mau pokhala choonadi, (Yohane 17:17) amatichenjeza ndikutikonza zolakwa zathu (2 Timoteo 3:16,17), choncho, sichingakhale chodabwitsa kuona kuti onse ambiri okhulupirira mu choonadi ichi ali anthu osatchuka, osauka, osawerengedwa komanso odedwa ndi dziko lapansi mu zochitika za tsiku ndi tsiku. Izi ziri chonchi popeza zochita za Mulungu zisiyana kwambiri ndi zochita za dziko lapansi. N'chifukwa chake, palibe amene amalabadira za anthu okonda Yehova otere kotero, chawo nkulandira mnyozo ndi chitonzoz komanso kuponderezedwa kumene kumalo antchito ndi kwina kulikonse chifukwa izi zimachitika mu nzeru za dziko lapansi. Chipulumutso chiribe gawo mu ntchito zotere choncho, anthu okhulupirirawa ayeneradi kutsamiza miyoyo yawo pa zoonza zokha zokha. Yeremiya anazuzika koposa ndipo anthu ambiri anamutsutsa chifukwa chokamba za Mau omwe Mulungu anamutuma, motero, analumbira kuti

sadzanenanso ndi kulalikanso Uthengawu kwa anthu. Koma popeza Mauwa anawuziridwa ndi Mulungu, ndipo kuti Mau akewo anali kukwaniritsa cholinga chake osati zofuna zake, Yeremiya iye anawumirizidwa *“...mokokedwa ndi kuwuziridwa ndi Mzimu Woyera”* koteru sanathenso kusankha koma kuchita chifuniro chake cha Mulungu. *“...Yehova, mwandikopa ine, ndipo ndinakopedwa; muli ndi mphamvu koposa ine, ndipo mwalakika; ine ndinakhala choseketsa dzuwa lonse, onse andiseka. Pakuti paliponse ndinena, ndimfuula, ndimfuula, chiwawa ndi chofunkha; pakuti mau a Mulungu ayesedwa kwaine chitonzo, ndi choseketsa, dzuwa lonse. Ndipo ndinati sindidzatchula Iye, sindidzanenanso m'dzina lake, pamene mtima mwanga muli ngati moto wotentha wotsekedwa m'mapfupa anga, ndipo ndalema ndi kupirira, sindingathe kupiriranso”* (Yeremiya 20:7,9). Ifenso tizifikako pamzere otopa ndi tchimo ndi kusaka saka Mau a Mlengiyo yemwe angatipatse chipulumutso monga anatsimikizira mu Mau akewo. Chimodzi modzinso pamene Balamu analakalaka kutonza ndi kutemberera Israeli, Mzimu wa Mulungu unatembenuza temberero lake ndipo mu malo mwake anapezeka kuti ananenera madalitso kwa ana a Israeli (Numeri 24:1-13 cp.Deuteronomo 23:5).

Chodabwitsa china ndi chakuti anthu angapo omwe Mulungu anawuzira kuti alankhule za Uthenga wake Wabwino kwa anthu ku Israeli, onse sanaulandire, sanakonzekere ndipo sanafune kutero atawuzidwa koyamba mpaka anawumirizidwa kufalitsa Uthengawu. Ena mwa iwo ndi anthu awa:

Mose	(Eksodo 4:10)
Ezekieli	(Ezekieli 3:14)
Yona	(Yona 1:2,3)
Paulo	(Machitidwe 18:9)
Timoteo	(1 Timoteo 4:6-14)
Balaamu	(Numeri 22:24)

Ichi chitsimikizira zomwe timaphunzira mu ndime ya Petro, 2 Petro 1:19-21 kuti Mulungu samalola kuti ife tichite ndikukwaniritsa zofuna zathu, koma

kuti, anthufe tiyenera tikwaniritse zolinga ndi zofuna za Yehova monga anzathu a chikhulupiriro'wa anawuziridwa ndi mpweya (Mzimu) wake polemba Baibulo. Mlozi (m'neneri) Amosi akukumbukira bwino motsimikizira ndikunena kuti “...*Ambuye Yehova wanena, ndiani amene sanenera?*” (Amosi 3:8). Nthawi zina ngakhale Mose ankasokera m'maganizo ndi mzochitika komabe anatsamira kwambiri pa *Yehova* “*Malamulo onse awa omwe Yehova ananena ndi Mose...*” (Numeri 15:22,23); mau awa ananenedwa ndi Mose mu ndime 17 (v.17).

Chitsimikizo china chikuwonetsa kuti olemba Baibulo nawonso sanathe kumvetsa nthawi zina zomwe ankalemba, motero, ankayesetsa kusanthula zomwe adalembezozo. Iwo “*anasanthula mamasulidwe ndi matanthawuzidwe... ndi kusanthula nthawi yiti kapena nthawi yanji Mzimu wa Khristu wokhala mwa iwo analozera*” (1 Petro 1:9-12), kusanthula izi zomwe zinalembedwazo iwo anafuna-funa mu umodzi. Mpfundo yomwe tingatolepo apa ndi yoti aneneri'wa ankalemba Mau owuziridwa ndi Mulungu, osati mwa iwo okha ayi, ndipo n'chifukwa chake kenaka anayambanso kusanthula Mau omwewo ngakhale anamasulira ndi iwo omwe. Ndime zotsatirazi ndi zina zomwe ziwonetsa motsimikiza pankhaniyi:- (Danieli 12:8-10; Zekariya 4:4-13; Petro (Machitidwe 10:17).

Anthu onsewa akanakhala kuti Mau a Mulungu sanali owuziridwa, pang'ono pakanakhala pobvuta kuti amalize kulemba Mau'wo mwandondomeko ngati momwe Mau'wa amamvekera lero. Koma chifukwa choti Mau'wa anawuziridwa, mau amene analembedwa ankachokera kwa Mulungu ndipo ntchito yonseyo inayenda bwino mwachifuniro chake ndi ndondomeko yake. Ntchito yonse inali m'manja mwa aneneri onse pamodzi ngakhale anali kumalo ndiponso kuti analemba m'miyoyo yawo pa nthawi yosiyana-siyana koma motsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Kotero, anakhala ngati akusidwa pamodzi kuti achite chinthu chimodzimodzi mogwirizana mpfundo zawo zomwe zinali zochokera kwa Mulungu. Kunali ngati kuyamba nkhani ndi m'neneri m'modzi n'kukamalizitsa ndi wina pa mpfundo yomweyo inayambidwayo. Kubvomereza kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu zimatiipatsa mphamvu, chilimbitso ndi chilakolako chowerenga ndinso kumvera zonse zomwe timawerengazo. “*Mau anu ngoyera ndithu; choncho, mtumiki wanu awakonda*” (Masalmo 119:140).

Mwaichi, mabuku a mu Baibulo ndintchito yolembedwa ndi Mulungu yomwe inagwiridwa mothandizidwa ndi Mzimu wa Mulunguyo ndipo mau'wo ndi

osiyana kwambiri ndi nthano komanso zolembedwa zina zonse padziko lapansi. Izi zimaoneka kwambiri pamene tiyamba kuganizira Chipangano Chatsopano mogwirizana ndi zolembedwa mu Chipangano Chakale:

- Mateyu 2:5 (R.V. mg.) akufotokozera m'mene Mau'wa analembedwera; “...*kunalembedwa kotere ndi m'neneri...*”– Mulungu ankalemba kudzera mwa aneneri. Mu Baibulo, timakonda kuwerenga kuti “..*analemba mwa aneneri*” ponena za m'mene Mulungu analemba Mau ake mu Baibulo pamene anali kulankhula kudzera mwa aneneri ake kalelo.
- “...*Mzimu Woyera unanena mwa mkamwa mwa Davide...*” (Machitidwe 1:16) Umu ndi momwe Petro ananenera pokumbukira mu Buku la Masalmo: (A Hebri 3:7).
- “...*Mzimu Woyera unalankhula kokoma mwa m'neneri Yesaya*” (Machitidwe 28:25- umu ndi m'mene Paulo ananenera pokumbukira zonedwa ndi Mulungu mwa Yesaya). Luka 3:4 alankhula za “...*mkalata ya mau a Yesaya m'neneri*” osati “*mkalata ya Yesaya*” ayi.

Zonsezi zikutanthauza kuti anthu akale sankawona za munthu yemwe walemba kapena kulalika Mau a Mulungu ayi koma m'mene uthenga wo wafikira kwa anthu amene adali “*wouziridwa* (ndi mpweya) *ndi Mzimu Woyera* (Mphamvu ya Mulungu)”. Choyambirira kuchitika pakati pawo chinali kuonetsetsa kuti chifuniro cha Mulungu chakwaniritsidwa. Izi ndi zimene zinali zofunika kwambiri pachikhulupiriro chawo. Kotero Mulungu ankakhutitsidwa ndi zochita za ambiri mwa iwo monga Abrahamu, Isake, Eliya, ndi ena otero. Ifenso titengere chitsanzo chimenechi chomwe anasiya anzathu amenewa.

Tiyeni tionepo ndime zingapo zomwe zikuonetsa kuti Mzimu wa Mulungu unaululidwa kwaife kudzera mu Mau ake olembedwa:-

- Yesu ananena mosazimbayitsa, “...*Mau amene ndalankhula ndi inu ndi Mzimu...*” (Yohane 6:63); Iye analankhula motere modzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu omwe ndi mphamvu ya Atate ake (Yohane 17:8; 14:10).

- Ife olandira Mau ake mu chiyero, amatchulidwa wobadwa mwatsopano ndi Mzimu (Yohane 3:3-5) komanso mu Mau a Mulungu (1 Petro 1:23).
- **“...Mau amene Yehova wa Makamu anatumiza mwa Mzimu wake mwa aneneri ake..”** (Zekariya 7:12). Nthawi zonse, tikuwerenga kuti Mulungu kudzera mwa Mzimu Wake, anatumiza Mau ake kuti akabveke kwa anthu okhala padziko.
- **“...Taonani nditsanulira painu Mzimu wanga; ndipo ndidzakudziwitsani Mau anga”** (Miyambo 1:23) mau otere akugwirizana kwathunthu kuti tiyenera kuzindikira Mau a Yehova kwambiri. Tidziwensho mphamvu yake (Mzimu Wake) ndinso zomwe mphamvuyo imachita pakati pathu. Kuwerenga Baibulo mosamvetsa bwino ndi kosathandiza konse, chifukwa mzimu kapena titi maganizo a Mulungu sadzawululika kwaife kotero, sitidzapindula chirichonse ndipo popeza Mau’wo sadzawululidwa, sangakhale ndi tanthawuzo lililonse mu moyo wathu.
- Pali kufanana kwambiri pakati pa Mau a Mulungu ndi Mzimu wa Mulungu. M’ndime zambiri za m’Buku Lopatulika: **“Mzimu wanga umene uli paiwe, ndi mau anga amene ndaika mkamwa mwako sadzachoka mkamwa mwako...”** (Yesaya 59:21); **“...chifukwa cha Mau ake ndi monga mwa mu mtima mwanu (mzimu) (2 Samueli 7:21); “...Ndipo ndidzayika Mzimu wanga mwa inu (mu mtima mwanu monga m’mene zalembedwera)...” “....ndidzayika chilamulo changamu mtima mwao”** (Ezekieli 36:27; Yereimiya 31:33).

MPHAMVU YA MAU A MULUNGU

Mphamvu ya Mulungu simaganizo kapena maonekedwe ake okha ayi komanso mphamvu ndinso nyonga zake zomwensho zikhoza kuwonekera m’chikhalidwe ndi chiganizo chake. Mwaichi, mphamvu ya Mau ake sinkhamba kamwa chabe ayi koma kuti ndi mphamvu zotsatira m’malondolozedwe a Mau ake. Tikhoza kunenanso kuti mphamvu zake ndi kalondo-londo wa Mau ake onenedwa kalelo. Tikakhutitsidwa ndikulola Mau ake, sitidzadandaula kapena kuda nkhawa ndi zokhumudwitsa zina zirizonse za m’dziko ayi, popeza nzeru zathu zowopa Mulungu m’chiyembekezo chake, zidzatipatsa mphamvu mu dzina lakelo, yogonjetsera mayesero onse omwe

angafune kutilepheretsa kulandira moyo wosatha. Monga mwa nthawi zonse, Paulo analemba:-

- **“...Pakuti Uthenga Wabwino** (Mau a Mulungu) **siundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyense wakukhulupirira**” (Aroma 1:16).
- Luka 1:37 (R.V.) akutsimikizira mpfundo yomweyi: **“...chifukwa palibe mau amodzi akuchokera kwa Mulungu adzakhala opanda mphamvu** (Mzimu)”.

Motero, tionanso kuti kudziwitsana, kuphunzitsana, kugawana ndi kukumbutsana Mau a Mulungu pakati pathu ngati anthu a chikhulupiriro, ndikofunikira. Sizifanana ndi maphunziro opitira kusukulu ya ubusa (Theology) ayi chifukwa tikamawerenga mu Baibulo, sitipezamo anthu a chiphunzitso opita ku masukulu otere ayi, koma chiphunzitso cha okhulupirira okha-okha kuti azilimbikitsana (Bible Study). Sizifanananso ndi kumangopita ku matcharitchi sabata iriyonse, ndikumadzinamiza kuti ndife a khristu pamene sitizindikira zambiri za Khristu Yesu, Mulungu, Mau ake ndi mphamvu zake ayi koma kudziwa mphamvu yakeyo ndipo mkuzindikirako, muli chilimbitso chachikulu. **“...pakuti Mau a Mulungu ali amoyo, a changu m’kuchita ndi mphamvu”; “...ndi Mau a Mphamvu yake...”** (A Hebrai 4: 12; 1:3). **“...Mau a Mulungu amenenso agwira ntchito mwa inu okhulupirira”** (1 Atesalonika 2:13). Kudzera m’Mau ake, Mulungu amagwira ntchito yayikulu zedi mwa anthu ake okhulupirira nthawi zonse.

Maphunziro ano kotero, ndi amene angakuthandizeni kukhala ozindikira komanso odalira pa Uthenga Wabwino choncho, mudzakhanso ndi Mphamvu ya Mulungu; Mukalola kuti zitero, Mau’wa adzakusinthani inu kuti mukhale mwana wa Mulungu. Mwana wa Mulungu woonetsa zizindikiro za Uzimu wa Mulungu mwainu, pokukonzaninsu inu, kukutsukani inu, n’kukusinthani kuti ndithu mukakhale m’kawonekedwe, makhalidwe ndi chinyezimiro cha Mulungu chomwe mudzakhala nacho pamene Yesu Khristu adzabweranso (2 Petro 1:4). Ulaliki wa Paulo **“...Siwunakhala ndi Mau a nzeru, koma m’chiwonetso cha Mzimu ndi cha Mphamvu....”** (1 Akorinto 2:4-5).

Lero tazunguliridwa ndi anzathu omwe chikhulupiriro chawo pa Baibulo n’choperevera ngakhale amalimbikira kuti anadzipereka kwa Yesu Khristu.

Koteronso, amanena kuti ndi okhulupirira Mulungu ngakhale chikhaliidwe chawo chili cholephera komanso salola uthunthu ndi maonekedwe ake. Amati ndi opulumutsidwa ngakhale kuti samadziwa tanthawuzo leni leni la Mphamvu yake. Pongokana mauziridwe a Mau ake ndi mapatulidwe ake mu umoyo wathu komanso mu zochita zathu, ndiye kuti takana Mphamvu yake ya Mulungu. Mau ake pa ndime ya 2 Timoteo 3:5 tikumbukira “...*akukhala nao maonekedwe a chipembedzo, koma mphamvu yake adayikana,*” i.e. Mphamvu ya Mau a Uthenga Wabwino.

Tsinde ndi maziko a chikhulupiriro chathu zakhala zikunyozedwa ndi kusekedwa padziko lino ndipo izi zinamuchitikiranso Paulo: “...*Pakuti Mau a mtanda ali ndithu chinthu chopusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tiri kupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu,*”(1 Akorinto 1:8).

Mozindikira ichi, kodi sityenera kukhala pansu mofatsa, kutenga Baibulo molemekeza podziwa kuti ndi Mau a Mulungu, ndikuwerenga kotero, tikamve ndikuzindikira mkuchita monga tamva? Tisatengeke ndi chigulu cha anthu ayi popeza Ambuye ananeneratu kuti khomolo ndi lopapatiza kotero, ambiri olowera pa khomo lolikululo sadzaona Ambuye pa mu Ufumu wake.

KUBVOMEREZA MAU A MULUNGU

Kawiri kawiri tikawerenga Mau a m’Baibulo, timatolapo chinthu chimodzi ndicho kuti amene analemba Mau a Mulungu ankazindikira kuti zimene akulemba iwo ndi zina zonse zomwe ankalemba anzawo zinali zowuluridwa ndi Mpweya wa Mulungu, kunena kuti anakhudzidwa ndi Mulungu polemba Buku Lopatulika. Ambuye Yesu analimbika koposa pa nkhani yomweyi pamene anathira ndemanga mmau a Davide nanena, “..*Davide mu Mzimu amtchula Iye bwanji Ambuye....*” (Mateyu 22:43); Apa Iye anaonetsa kuti mau a Davide mu Masalmo anali owuziridwa ndi Mulungu. Yesu ananenso za Mose “...*Pakuti mukadakhulupirira Mose, mukadakhulupirira Ine; pakuti iyeyu analemba za Ine....*” (Yohane 5:45-47), kuonetseratu kuti ngakhale Yesu anakhulupiranso kuti Mose ndi amene analemba mabuku asanu oyamba a mu Baibulo. Onani kuti akhristu ena odzikweza amakana kuti Mose ndiye amene analemba mabuku asanu aja oyambirira mu Baibulo koma Yesu Mwini akusiyana ndi maganizo ochepa otere pobvomereza kuti Mose ndi amene analemba mabukuwa. Iye anawatchula malembo a Mose “..*lamulo la Mulungu...*” (Marko 7:8,9). Ena ambiri amati Chipangano Chakale ndi nthano

chabe, si mau a Mulungu, koma Yesu ndi Paulo amatitsimikizira kuti ndi Mau eni eni owuziridwa ndi Mlengi; Yesu pokamba za mpfumakazi ya ku Sheba ananenetsa kuti ndi zinthu zomwe zinachitika ndithu ndipo kuti mpfumakazi'yu adzayankha mlandu wake pamaso pa Iye (Mateyu 12:42); sananene kuti *“monga nthano ya mpfumakazi ya ku Sheba”* ayi. Zindikirani kuti inabwera Yesu asanabadwe.

Atumwi nawonso anabvomereza kwathunthu mfundo imeneyi yomwe Yesu anakhulupirira. Izi tingazione mwa mtumwi Petro yemwe anati *“...pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwida ndi Mzimu Woyero, analankhula”* (2 Petro 1:19-21). Petro anakhulupirira kuti makalata a Paulo anali *“Mau a chiyero cha Mulungu”* ndipo kuti monga mwa Mau a Mulungu onse; Chipangano Chakale sichinasiyane ndi Mau a mu Chipangano Chatsopano. Onse agona pa malamulo a Mulungu.

Olemba Chipangano Chatsopano monga Machitidwe a Mtumwi, makalata a Paulo ndi Chibvumbulutso amatsimikizira zoti ndi *“Uthenga Wabwino”* (Machitidwe 13:51); Mateyu 10:14), kuonetsa kuti onsewa anawuziridwa kapena titi kugwidwa ndi Mzimu Woyera umodzi womwe'wo. Paulo mu ndime ya 1 Timoteo 5:18 akutikumbutsa tonsefe kuti zolembedwa pa Deuteronomo 25:4 (m'Chipangano Chakale) ndi Luka 10:7 ndi *“Mau a Mulungu”*. Paulo akunenanso motsimikiza kuti zonse zomwe iye akulalika ndizochokera kwa Yesu Khristu osati mwaiye yekha ayi (Agalatiya 1:11,12; 1 Akorinto 2:13; 15:3). Tikaona zonsezi tizindikira kuti zinali zobvomerezeka ndi pamaso pa atumwi ena onse monga; Yakobo 4:5 akunenanso nkhani yotere pokambapo za mau a Paulo kuti ndi *“Uthenga Wabwino wa Mulungu”* kuthirira ndemanga Agalatiya 5: 17.

Mulungu analankhula kwambiri kwaife kudzera mwa Khristu Yesu; koteri palibe chifukwa choti tifune funenso umboni wina wapadera (A Hebrai 1:2). Tingawonenso kuti Baibulo limakambapo za Mau ena omwe sanaphatikizidwe mu Buku Lopatulikali (monga buku la Yasha [Jasher], zolembedwa ndi Natani, Eliya, Paulo ku Akorinto; ndi kalata yachitatu ya Yohane imanena kuti Yohane analemba kalata yomwe siyinasungidwe komanso yomwe Diotirifesi sanamvere malangizo ake). Chifukwa chiyani Mau otere sanasungidwe ndi kuwuluridwa kwaife? N'zowonekeratu kuti mau'wa sanali ofunikira kweni

kweni kwaife. Kotero, tiyenera kutsimikizira kuti zomwe zinasungidwazo ndi zomwe Mulungu anafuna kuti ife tizidziwe ndi kuzigwiritsa ntchito.

Timamva kuti mabuku ena mu Chipangano Chatsopano anangoledwa kuti akhale Mau a Mulungu, zikanakhala choncho sizikanatheka kuti olemba mabuku ena aja abvomerezeke kuti buku lowuziridwa ndi mphamvu ya Mulungu lifanane ndi buku wamba ayi. Iwo ngati ogwidwa ndi Mzimu Woyera ankatha kuonanso momwe Mulungu ankapereka Uthenga Wake kwa aneneri anzawo. Panali mphatso ya Mzimu Yomwe inathandiza kuunika ndi kusankha Mau a Mulungu eni eni kusiyantsa ndi Mau a munthu wamba mwa Mphamvu Yakeyo (1 Akorinto 14:37; 1 Yohane 4:1; Chibvumbulutso 2:2). Izi ziwonetsa kuti ngakhale makalata onse aja anali owuziridwa ndi Mulungu chifukwa choti anabvomerezedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Zikanakhala kuti mau a munthu wamba analoledwa mu Baibulo, Buku Lopatulika lero silikanakhala Buku Loopeka ndi Lolemekezedwa pakati pathu, silikanakhala ndi ulemerero omwe ulipo'wu.

2.3 MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Nthawi yambiri yomwe Mulungu wakhala akulankhula ndi anthu ake, ankatuma “Mzimu wake Woyera” kwa anthu. Ngakhale izi zinali choncho, sikuti zinkangopangika pachabe ayi; Kugwiritsa ntchito Mzimu Woyera kunali ndi cholinga chapadera ndi Mwiniyo. Cholinga chimenechi chitakwaniritsidwa, ‘Mzimu Woyera’ uja unalandidwa ndikuchotsedwa pakati pathu. Tikumbukire kuti cholinga cha Mulungu chinali ndi Iye m’magano ake kotero kuti “Mzimu wa Mulungu Woyera” unkachita zonse monga mwamaganizo a Mwini wakeyo. Tikaona cholinga chake, tidzazindikira kuti ndi chomwe chinabweretsa kusakhutira pakati pa anthu omwe nthawi zonse amafuna kuchita zofuna zawo. Tidziwanso kuti cholinga cha Mulungu chimabweretsa mabvuto pakati pa okhulupirira koma chosangalatsa kwambiri ndi chakuti, kwa okhulupirirawo, mabvuto amene’wa akatha (Yesu akadzabwera) komaliza kwake ndi chisangalalo. Kotero zochitika zonse lero zimakwaniritsa cholinga cha Mulungu monga Mwini analemba m’Buku Lopatulika (onani Phunziro 6.1). Tikawerenga ichi, timvanso kuti sicholinga cha Mulungu kuchotsa mazunzo pakati pathu mu moyo uno ayi, koma kuti

atha kuchita izi pofuna kulozera ndikukwaniritsa zomwe Iye afuna zichitike mtsogolomo kotero ife tikamdziwe Mulungu Wathu monga anachitira ndi ana a Israeli kalelo.

Izi zikusiyana koposa ndi m'mene akhristu ambiri amadziwira za Mzimu Woyera lero; mwachitsanzo, akhristu ambiri amati chikhulupiriro mwa Yesu Khristu chimabweretsa machiritso kumatenda osiyana siyana nthawi yomweyo, ngakhale munthu odwalayo sakumudziwa kokwanira Yesuyo! Amati Mzimu Woyera umachiritsa matenda komanso utha kumuthandiza munthu kuti alemere chachikulu akhulupirire basi. N'chifukwa chake timamva kumayiko komwe kuli nkondo zachiwani-weni monga Uganda, Sudani, Zaire kuli anthu ambiri omwe amati ali ndi mphatso ya Mzimu Woyera ya machiritso; mwatsoka, amapezana ndi anthu oti ataya kale mitima yawo chifukwa cha mabvuto osiyana-siyana. Kotero, amakhulupirira msanga chifukwa chofuna mtendere. Koma kodi mtendere ndi machiritso otere'wa amawapezadi? Tiona nthawi zambiri kuti sizikhala choncho. Si anthu ambiri omwe amakhulupirira zotere kuti zikuchitikadi kotero amangololera pofuna kusangalatsa omwe akulalika mau otere'wa. Ngati munthu wina atafuna kuti afufuze bwino za zipolowe ndi mabvuto omwe akuchitika lero'wa n'kosabvuta kupeza mayankho ake m'Baibulo ndipo atha kukhutira kuti Mau a Mulungu sapita pa chabe.

“...Akhristu” ambiri lero amanena kuti ali ndi mphatso za Mzimu Woyera za machiritso ndi zina zotero koma zachisoni, sadziwa cholinga cheni cheni cha Mzimu Woyera panthawi imeneyo. Mulungu ankagwiritsa ntchito Mzimu wake Woyera m'njira yomwe Iye Mwini anakonzeratu mwapadera kuti zotsatira zake zioneke bwino. Mwanjira iyi, onse amene anali ndi Mzimu Woyera umenewu, ankatha kupanga zinthu zomwe iwo eni ankadziwa kuti anayenera kuchita pa nthawi yopatulika komanso mwapadera momwemo. Zonsezi zinkachitika mogwirizana ndi maganizo a Mulungu kotero kuti ntchito yotere inakwaniritsidwa mu cholinga cheni-cheni cha Mwini wakeyo. Tiona kuti apa zomwe zikuchitika masiku anozi ndi zosiyana kwambiri ndi m'mene anzathu omwe adalandira Mzimu Woyera kalelo ankadziwira; Masiku ano, Mzimu Woyera wa akhristu a lero, samatha kuchiritsiratu matenda, sangathe kuutsa munthu wakufa monga zinaliri ndi anzathu kalelo. Anthu okhala ndi Mzimu wa Mulungu lero amapempherera munthu wodwala, wakufa maola ambiri-mbiri koma osachila, munthu wakufa osauka kuimfa! Chizindikiro cheni cheni chowonetsa kusoweka kwa mphamvu yeni yeni ya Mulungu.

Zitsanzo ziri m'munsizi zionetsa zifukwa zapadera zomwe Mzimu unkatumizidwira kwa anthu kuti akhale ndi mphatso zosiyana-siyana za Mzimu Woyera. Mzitsanzo zonsezi, palibe zomwe zikuonetsa kuti anzathu aja anagwiritsapo ntchito Mzimu Woyera omwe anali nawo pokwaniritsa zilakolako zawo. Ichi ndichifukwa chakuti anthu'wa ankazindikira kwathunthu cholinga cha mphamvu yapaderayi yomwe ndi Mzimu Woyera wotumizidwa kwa iwo ndi Mulungu. Iwo anadziwa kuti Mulungu anali ndi ntchito yapadera kuti akwaniritse mwa iwo powapatsa Mzimu Woyera kusiyana ndi ena mwa aneneri omwe anawapatsa mongoyembekezera (Yesaya 40:13).

- M'mbiri yakale ya ana a Israeli: anthu anawalamula kuti amange **“chihema”** momwe ankayikamo guwa ndi zinthu zina za nsembe; Panali njira ndi malamulo a mphamvu omwe anakhazikitsidwa popanga zinthu zotere n'cholinga chofuna kupembedza Mulungu m'chowonadi. Kuti njira zimenezi zitsatidwe, Mulungu anayikapo Mzimu Wake kuti uhandize anthu amene ankapanga zinthu za mtundu wotere mu chihemacho. Iwo **“...amene ndawadzaza ndi Mzimu Wanzeru paluso, kuti amusokere Aaroni zobvala...”** (Eksodo 28:3).
- M'modzi wa anthu amene'wa, Bezaleli, **“...anamudzaza ndi Mzimu wa Yehova M'nzeru zakudziwa, kuzindikira ndi ntchito zirizonse, kulingalira ntchito zaluso, kugwira ntchito ndi golide, siliva ndi kudula miyala ina yapamwamba m'ntchito zonse”** (Eksodo 31:3-5). Onani kuti pafupi-fupi chinthu chirichonse chiri ndi mzimu (mphamvu) wake wake ndipo munthu akatumidwa ndi Mulungu kuti achite chimodzi mwa zinthu zimenezi, ankapatsidwa mphamvu ya chinthucho.
- Numeri 11:14-17 analemba za Mzimu womwe unapatsidwa kwa Mose ndipo unachotsedwanso kwa Iyeyo nuperekedwa kwa akulu-akulu a ana a Israeli, pofuna kuwathandiza akulu-akuluwo kukhala ndi nzeru zapadera zoweruzira milandu pakati pa anthu aku Israeli, mwa njira iyi, ntchito ya Mose inapepuka. Mose atatsala pang'ono kufa, Mzimu Wake unapatsidwa kwa Yoswa koteru kuti iyenso athe kutsogolera ana a Israeli omwe ndi ana a Mulungu (Deuteronomo 34:9)
- Kuchokera pomwe ana a Israeli analowa mu dziko lawo la Kanani mpaka pamene anakhala ndi mfumu yawo yoyamba (Sauli), iwo ankatsogoleredwa ndi Oweruza okha basi. Nthawi imeneyi kawiri kawiri ankazungulira ndi adani awo owazungulira, koma timamva kuti Mzimu wa

Mulungu unkawakuta ena mwa oweruzawo kotero, Israeli amatha kuwomboledwa kwa adani aja;- zitsanzo za ena mwa oweruza'wa ndi awa: Otiniyeli (Oweruza 14:19), Gideoni (Oweruza 6:34) ndi Yefita (Oweruza 11:29) ndi ena otero.

- Oweruza wina Samsoni anapatsidwa Mzimu (mphamvu) kuti aphe mkango (Oweruza 14:5,6); kupha anthu makuni atatu (30) (Oweruza 14:19), kudula zingwe zolimba zomwe anamumangira nazo (Oweruza 15:14). Mzimu Woyera wotere sitinganene kuti Samsoni ankakhala nawo nthawi zonse ayi, Unkachita kubwera pa nthawi yomwe chinthu chofunikira ngati zanenedwazi zikafika. Panali nthawi ina pomwe Mzimu wotere unkachotsedwanso ndipo timawerenga kuti pa nthawi yotere, anzathu omwe analandirapo Mzimu wa Mulungu wotere, ankagwada pansu kupemphera kuti ngati nkutheka, mphamvu ya Mulungu igwirensa ntchito.
- Mulungu akakhala ndi Uthenga wapadera kwa anthu ake, Mzimu wake unkatha kumudzera munthuyo ndikulankhula zomwe Mulungu wamutuma. Mau aja akalankhulidwa m'malo mwa Mulungu anthu naamva, Mzimu uja unkamuchoka ndipo munthu uja amayambanso kulankhula mwa umunthu wake. Pali zitsanzo zambiri zomwe zingaperekedwe zoonetsa momwe Mzimu Woyera unkawachokera anthu, monga Samsoni unamchokerapo Mzimu atameta tsitsi lake. Zitsanzo zina nazi:-

“....Ndipo Mzimu wa Mulungu unavakidwa kwa Zakariya..naanena nawo, Atero Mulungu, mulakwilanji malamulo a Yehova...?”

Onaniso 2 Mbiri 15:1,2 ndi Luka 4:18,19 kuti muzindikire bwino zitsanzo zina pa zomwe mwawerenga mu gawo lino. Muona kuti zambiri zomwe akhristu ambiri amakonda kulalika zimasiyana kwambiri ndi zomwe mungawerenge panokha mu Baibulo.

Monga tawerenga, tiona kuti mphatso ya Mzimu wa Mulungu unkapatsidwa ndi Mulungu pofuna kukwaniritsa cholinga chake ndi ntchito ina yapadera. Osati:

- Ngati chotsimikizira kuti wina ndi wopulumutsidwa
- Wakhazikika mwa munthu moyo wake wonse
- Chinthu chapadera choopsa mwa munthu ayi
- Chinthu chongobwera nthawi ina iriyonse mwa munthu akafuna ayi koma kudzera mu chifuniro cha Mulungu.

Chikonzero cha Mulungu mkalandiridwe ka Mzimu Woyera chikusiyana kwambiri ndi m'mene akhristu a lero amalandirira komanso zolinga za Mzimu Woyera lero sizimadziwika bwino pamene nthawi imeneyo zinkadziwika monga tawerengera m'mwambamu. Mwa akhristu a lero, mphatso za mzimu ikhoza kukhala iripo koma kodi mzimu wake ndiwo uti? Nanga mphatso zake ndi ziti ndipo ndizochokera kuti? N'chodziwikiratu kuti ambiri mwa akhristu otere samazindikira zomwe mphatso ya Mzimu Woyera imatanthawuza ndikutinso Mzimu'wo ndichiyani? Tawerenga kuti Samsoni anapatsidwa Mzimu kuti aphe mkango (Oweruza 14:5,6); pamene anaonana maso ndi maso ndi mkango woopsawo koma Samsoni sanachite mantha chifukwa anadziwa kuti Mzimu womwe anali nawo ndi omwe ugonjetse mkangowo. Sanakayikire kuti ichi chichitika. Zosiyanadi ndi m'mene mzimu woyera wa lero ukugwirira ntchito ngati imeneyi. Mwaichi, ndikobvuta kunena kuti tiri ndi Mzimu Woyera weni weni lero womwe sukhala ndi ntchito kapena cholinga chenicheni mwandondomeko choti chichitike ngati momwe zinaliri kalelo.

Sitichitira mwina koma kunena kuti chikhristu chotere ndi chonthunthumira pa zinthu zopanda pake, zopanda maziko ake eni eni omwe ayenera kutsamira pa Baibulo. Sibwino kupezerapo mwayi pogwiritsa ntchito ndime zochepa za mu Baibulo kuti tikwaniritse zolinga zathu za mu dziko ayi. Nchifukwa chake munthu olandira Mzimu Woyera lero amachimwa mwina kuba kaya chiwere-were chimene popeza ali ndi Mzimu wakufa osiyana kwambiri ndi umene unali pa nthawi'yo. Tiyeni tionetsetse chinthu chimodzi ndicho, kuzindikira mozama kuti munthu sangalandire chipulumutso asanazindikire kweni-kweni zomwe Baibulo limatiphunzitsa. Ndongomeko yake ndiyo; kumva Mau a Mulungu, kuwerenga ndi kutsimikizira zolalikidwazo ngati ndi zoono, kuzindikira, kukhulupirira, kugwirizana nazo kenaka ndikubatzidwa. Kutembenuka mtima kotere ndiko koyenera komanso kogwirizana ndi chilongosoko cha Mau a Mulungu.

Pamene tikulimbana ndi chinyengo cha dziko lapansi (Yeremiya 17:9), maka mkati kati mwa akhristu, tiyeni abale ndi alongo tilimbe potsata chiphunzitso cha Baibulo lomwe ndi Mau eni-eni a Mulungu. Tilimbikire maphunzira athu monga tikuchitiramu choncho tidziwe kokwanira kotero tikalumikizane ndi chilongosoko, monga momwe Baibulo limafotokozera za Mau osiyana siyana ngati omwe tikuphunzira'wa. Tikhoza kumaona ngati Mzimu Woyera ukugwira ntchito mwaife lero ndi kumadzimva ngati mphamvu'yo imakhala ndi ife nthawi zonse kuti titchinjirizidwe mu machimo. Koma izi zingachitike bwaji? Kodi ife lero timakhaladi ndi Mzimu Woyera monga m'mene ankachitira anzathu kale lija? Ngati tifunitsitsa kumudziwa Mulungu mu choonadi, tidzayesetsa kufuna-funa pophunzira za Iye kuti timudziwe bwino.

ZIFUKWA ZOMWE MULUNGU ANATUMIZIRA MZIMU WAKE WOYERA MU CHIRUMIKA CHOYAMBA

Poona kuti tsopano taphunzira m'mene Mzimu Woyera unkatumizidwira, ndipo tadziwa kuti Mzimuwo ndi chiyani, nanga cholinga chake chinali chiyani, tiyeni tsopano tiganizire za momwe Mzimu Woyera unafikira kwa anzathu a mu Chipangano Chatsopano, komanso tione momwe mphatso za Mzimu zinkagwirira ntchito Yesu atakwera kumuka ku mwamba.

Lamulo lomaliza la Yesu kwa akuphunzira ake, linali loti amuke kudziko lonse kukalalikira "Uthenga Wabwino" (Marko 16:15,16). Ichi anachita, potsamira kwambiri ulaliki wao pa kufa ndi kuukanso kwa Ambuye Wathu Yesu Khristu. Koma tikumbukire kuti nthawi imene ija kunalibe Chipangano Chatsopano mu Baibulo. Pamene atumwi ankalalika za Yesu mu misewu, misika, mu masunagoge (kachisi) ozungulira Nazareti, zolalika zawo zinkakhala ngati nkhabakamwa chabe; kukamba za kalipentala wamba waku Israeli yemwe anali wosachimwa, wopanda banga, naafa ndipo anaukanso kwa akufa, nakwaniritsa za aneneri mu Chipangano Chakale; moganizira ichi, anthu akufunsidwa kuti abatizidwe potsata chitsanzo chake mu ubatizo weni weni. Yesu anapereka chitsanzo cha ubatizo umenewu pobatizidwa mu m'tsinje wa Yordano. Mkalata yake kwa Aroma Paulo, anatsimikizira za ubatizo weni weni wotere womwe Yesu anabatizidwa ngati chitsanzo chimene ife tiyenera kutsata lero (Aroma 6:1-6).

Nthawi imeneyo, anthu ena ankayesa yesa kulimbikitsa chipembedzo cha mizimu (chikunja). Kudali koyenera kukhala ndi njira yeni yeni yachitsanzo chabwino yowonetsa kuti ungiro wa Mau a Mulungu ulipo m'malalikidwe ndi m'makhalidwe a ana a Israeli.

Lero timatsamira pa Mau a mu Chipangano Chatsopano pofuna kutsimikizira kudalirika kwa zolalikira zathu kuti ndithu ndizochokera kwa Mulungu; Masiku amenewo, Chipangano Chatsopano chisanalembedwe, Mulungu analola Mzimu Woyera ulalike kudzera mwa alaliki omwe Iye Mwini anawasankha nayikapo dzanja lake. Ichi ndiye chifukwa cheni-cheni chimene Mulungu anatumizira Mzimu Woyera womwe ndi Mphamvu Yake yapadera yokhala ndi mphatso zosiyana siyana ndi cholinga chothandiza kulemba Uthenga Wabwino mu Chipangano Chatsopano. Kusoweka kwa Chipangano Chatsopano kukanadzetsa mabvuto ambiri pa mafalitso a Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu kotero, akhristu oyambirira sakanakhala m'moyo wawo wa chikhulupiriro mu Uzimu. Zikadakhala zobvuta kuthetsa zopsyinja zambiri zimene zidabwera nthawi imene ija chifukwa chosamvetsa ndi kusadziwa choyenera kuchitika pachipembedzo chirichonse popanda Buku Lopatulika, la ndondomeko komanso lolongosola machitidwe a zinthu mu chikhristu choyenera. Izi zikanakhudzanso umoyo wathu wachikhristu lero. Tiyenera kuyamikira kuti tiri ndi "Uthenga Wabwino" onse pakati pathu kotero, tikalakwitsa timakonzedwa mu mitima mwathu ndi chiyembekezo chomwe chiri mu Baibulo lathu. Machiritso, malirime, maukitsidwe ndi zina zozizwitsa zambiri momwe mumaonera mphamvu ndi chitsimikizo cha Mau ake a Mulungu kotero, anthu anakhulupirira kuti Mulunguyo anali ndi iwo onse; ndipo kuti ifenso lero tikhulupirira izipopanda chikayiko china chirichonse. Mphamvu ndi mphatso za Mzimu Woyera zonsezi, zinali zoyenera ndi zofunikira kuti zipereke chitsimikizo ndi chikhulupiriro komanso kuti zikhale ngati mlozo wa moyo wachikhristu mu nthawi yoyambirira ija, mpaka pamene Chipangano Chatsopano chinapezeka pakati pawo, kudzera mwa atumwi omwe anawuziridwa ndi mpweya wa Mphamvu ya Mulungu. Chifukwa cha ichi, lero tiri ndi Chipangano Chatsopano chomwe chimatiphunzitsa chiphunzitsa ndi chilimbikitso cha Yesu Khristu yemwe ali Mwana wa Mulungu.

Mongofuna kukumbutsana, Baibulo limatifotokozera nkhani ya mtundu umenewu mu ndime zotsatira ziri m'munsizi:

- **“..m'mene anakwera (Yesu) kumwamba, ndipo anapatsa...(Mzimu) kwa anthu, mphatso za uneneri, ulaliki...kuti akonzere oyera mtima, muntchito ya (chiphunzitso) chipulumutso, ku thupi lonse la Yesu Khristu (okhulupirira) (Aefeso 4:8,12). Thupi la Yesu apa likutanthawuza Mpingo wa Yesu Khristu omwe ndi okhulupirira mu dzina lake. Ife tikakhulupirira timasandulika, kukhala chimodzi mwa ziwalo za thupi lake. Timanyamula mtanda wa Khristu mu mazunzo kotero timamva naye pamodzi ululu omwe Iye anawumva pantanda paja.**
- Mongoganiziranso izi, Paulo analembanso mkalata yake yopita kwa Aroma, **“...Pakuti ndilaka-laka kuonana ndiinu mukakhazikike” (Aroma 1:11). Kukhazikika mu chikhulupiriro chake mdongosolo komanso mogwirizana ndi Mau.**

Ponena za mphatso yapadera, kutsimikizira chiphunzitso cha Uthenga Wabwino mu ndondomeko yake monga Iye Mwini anakonzera pachiyambi, timawerenga:

- **“...Kuti Uthenga Wabwino sunadza kwainu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, komanso m'chitsimikizo ndi mkuchuluka kwakukulu kudzera m'machitidwe ndi machiritso a Khristu....”(1 Atesalonika 1:5 cp. 1 Akorinto 1:5,6).**
- Paulo anatha kunena za **“....zimene Khristu sanazichita mwa Ine zakumveretsa anthu amitundu, ndi mau ndi ntchito, mu Mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa, mu Mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa kulalikira Uthenga Wabwino wa Khristu” (Aroma 15:18,19).**
- Mokhudzana ndi olalikira Uthenga Wabwino, tiwerenganso, **“...Mulungu anatilibikitsa ife ndikuchitira umboni pamodzi nao mzizindikiro ndi zozizwitsa ndi mphamvu za mitundu-mitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa chifuniro chake” (A Hebrai 2:4).**

- Ulaliki wa Uthenga Wabwino ku Kupro (Cyprus) unamveka mothandizidwa ndi machiritso ndi zozizwitsa za Mzimu Woyera ndipo mwaichi, “.....*Pamenepo kazembe pakuona chochitikacho anakhulupirira, nabadwa nacho chiphunzitsa cha Ambuye,*” (Machitidwe 13:12).

Motsata izi, machiritso ndi zozizwitsa, zinamukhudza ndipo analemekeza chiphunzitsa cha Uthenga Wabwino. Ku Ikoniyo, “...*Ambuye amene anachitira umboni mau a chisomo chake, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zichitidwe ndi manja awo...*” (Machitidwe 14:3). Mazizwitso analidi njira yomanga ulaliki Wamphamvu. Zonse izi zalongosoledwa mwachidule mu ndemanga pa chitsanzo chomwe akuphunzira ake a Khristu anawonetsa pomvera malamulo kuti akalalike Uthenga Wabwino: “*Ndipo iwowa anatuluka, nalalikiraponse-ponse, ndipo Ambuye anachita nawo pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikiro zotsatirazo...*” (Marko 16:20).

Muzindikire kuti ulaliki wao unkatsimikizidwa ndi zizindikiro komanso zozizwitsa zimene olalikawo ankachita, asanayambe, mkati-kati mwa ulalikiwo, kapenanso atatha kulalika Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu; Panalibe ophunzitsa kapena kutsogolera anthu kulankhula m’malirime monga mipingo yatsopano imachitira ayi. Kale, kunalibenso zoti munthu apulumutsidwe asanazindikire Mau a Mulungu ndi kukhulupirira. Ndipo mukhoza kutsimikizira kuti lero ndondomeko yotere sikuonekanso m’chikonzero cha chipulumutso, machiritso ndi zozizwitsa za mipingo yosiyana siyana ya masiku ano. Kodi izi abale ndi alongo, zikugwirizana ndi chikonzero cha Mlengi Wathu monga timawerengera mu Baibulo?

ZINTHU ZAPADERA PA NTHAWI YOPATULIKA

Zipatso izi za Mzimu Woyera zidaperekedwa ndi cholinga chofuna kuchita zinthu mwapadera maka-maka kufalitsa Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu wa Ufumu wa Kumwamba panso pano mu nthawi yopatulidwa. Motero, tiona kuti nkulakwa kwakulu kunena kuti Mzimu Woyera ukadalandidwa mpaka lero ndipo kuti ziri choncho ngakhale masiku ano mpaka muyaya pomwe zipatso zake sizikuoneka. Akuphunzira ake a Yesu kuphatikizapo Petro, “...*anadzozedwa ndi Mzimu Woyera*” pa mwambo wa Pentekositi, Yesu atangokwera kumene kupita kumwamba (Machitidwe 2:4). Anathandizidwadi kulankhula mu malirime, zilankhulo zakunja pofuna kufalitsa Uthenga

Wabwino mozizwitsa. Anthu a maudio atayesetsa kutsekereza ufalitsa wa Uthengawu, “.....*Petro, modzazidwa ndi Mzimu Woyera*” *anawayankha mopanda mantha ndi momveka bwino*” (Machitidwe 4:8). Pongowatulutsa m’ndende, anathandizidwa ndi Mzimu Woyera, kupitiriza ntchito yofalitsa Uthenga- “...*ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula Mau a Mulungu molimbika mtima* (mopanda mantha kapenanso kunjenjera)” (Machitidwe 4:31).

Wophunzira weni-weni wofuna kudziwa Buku Lopatulika mwachindunji, akamawerenga mofatsa za akhristu oyamba, adzazindikira kuti sanali “...*odzazidwa kale mokhazikika ndi Mzimu Woyera*” pochita zinthu zimenezi. Ankachita kudzozedwa ndi Mphamvuyi pokha-pokha pakakhala zinthu zina zomwe Mulungu Mwini waona kuti ndizofunikira kuti zikwaniritsidwe, kenaka Mzimu uja unkawathera ndipo unkabweranso pakafunikira kukwaniritsa cholinga china cha Mulungu. Paulo moteronso “...*anadzozedwa ndi Mzimu Woyera*” pamene anabatizidwa koma patapita nthawi, “...*anadzozedwanso ndi Mzimu Woyera*” pofuna kulanga munthu wina wodzazidwa ndi uchimo ndi chilango cha khungu (Machitidwe 9:17; 13:9).

Pokambapo za Mphatso zozizwitsa za Mzimu, Paulo analemba kuti okhulupirira oyamba analandira Mzimu Woyera “...*monga mwa muyeso wa Mphatso ya Khristu...*” (Aefeso 4:7). Mu chi Greek, liwu lomwe latanthawuzidwa “*muyeso*” limatanthawuza kuti ndi “mbali ya chinthu chopatulidwa ndi kulingidwa mwapadera.” Motero, ndi Yesu yekha yemwe anali ndi Mphatso ya Mzimu yopanda malire, poyigwiritsanso ntchito monga an’kafunira Iye Mwini koma mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu (Yohane 3:34).

M’masitanza otsatira’wa, tiyeni tsopano tione Mphatso za Mzimu Woyera ngati momwe zinkagwirira ntchito mu masiku oyambirira’wo.

MPHATSO ZA MZIMU MCHIRUMIKA CHOYAMBA

Tanthawuzo la liwu loti “prophet (kapena kuti m’losi)” m’chi Greek limayimira munthu amene ankalalikira Mau a Mulungu polosera zakutsogolo mowuziridwa (2 Petro 1:19-21). Mwaichi, iwo amene anali ndi mphatso ya Ulosi “...*anatsika ku Yerusalemu kudza ku Antiyokeya. Ndipo anayima m’modzi wa iwo dzina lake Agabo, nalosa mwa Mzimu kuti padzakhala*

njala yaikulu padziko lonse lokhalamo anthu; ndiyo idadza masiku a Klaudiyo. Ndipo akuphunzira, yense monga anakhoza, anatsimikiza mtima kutumiza zothandiza abale akukhala m'Yudeya;" (Machitidwe 11:27-29). Uneneri wapamwamba wotere womwe unali kukwaniritsa ulosi wapadera, umasowa lero lino kwa anzathu amene amati ali ndi mphatso ya uneneri kapena titi ulosi; apa timawerenga kuti akhristu oyambirirawo adali wotsimikizira ndipo anali kuchita zinthu mowonetsadi kuti ndi odzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo kuti anadzipeka pogwiritsa ntchito nthawi, mphamvu ndi ndalama zawo pa ntchito yokomayi ndi cholinga chopepuza masautso amene analosedwawo. Zonsezi sitinganene kuti zikuchitikadi lero.

MACHIRITSO

Poganizira kuti atumwi aja ankalalika Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu kotero dziko lapansi liyeretsedwe, kunali koyenera kuti ulaliki wawo ulumikizidwe ndi chilimbitso cha machiritso mwa Mzimu, kuti anthu awone chitsanzo chabwino momwe zidzakhali mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo. "...maso a akhungu adzatsegulidwa, ndi makutu a ogontha adzatsegulidwa. Pamene wopunduka adzadumpha ngati nswala, ndi lirime la osalankhula lidzayimba nyimbo." (Yesaya 35:5,6-7). Imvani zambiri za Ufumu wa Mulungu powerenga Phunziro 5. Pamene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwe padziko lapansi, malonjezano onse ngati amenewa adzakwaniritsidwa mokwanira monga mwa malembo, ndipo sipadzakhalanso zoufufuza apa ndi apo ayi. Monga machiritso anawonekera kwa anthu onse padziko lapansi, kotero Ufumu wa Mulungu udzawonekeranso kwa onse olandira Mau a Mulungu.

Chitsanzo chachikulu tingachipeze powerenga za machiritso a munthu osayenda chibadwire yemwe ankamuyika pa Khomo Lokongola ndipo adachiritsidwa ndi Petro. Machitidwe 3:2 akunenetsa kuti munthuyu ankamuyika pakhomo lolowera tsiku ndi tsiku kotero, sanali wachilendo kwa anthu omwe ankapitapita ku sunagoge. Pochiritsidwa ndi mphatso ya Mzimu Woyera mwa Petro, iye anadumpha nayima, ndi kuyenda molowa mu sunagoge ndi iwo, ndipo anthu onse omwe amamudziwa anamuona iye akudumpha nalemekeza Mulungu: ndipo anamudziwanso kuti ndithu ndi yemwe uja ankapemphetsa tsiku ndi tsiku pakhomo paja. Mwaichi, anthu onse anadabwa ndikuzizwidwa pachimene chinachitika ndi munthu uja. Ndipo tiwerenganso kuti wopunduka uja anamugwiritsitsa Petro osamutaya pamene

anthu ambiri anathamangira kumene kunali iye, namuona modabwitsa, iye akunyadira ndi chimwemwe (Machitidwe 3:7-11). Izi ndi zosiyana kwambiri ndi m'mene mphatso za Mzimu wa lero ukugwirira ntchito ya Mulungu.

Petro anapezerapo mwayi wolalikira kwambiri za kuukanso kwathupi kwa Yesu Khristu. Onani kuti Petro anali nacho kale chilimbitso ndi chitsanzo chokwanira pochiza munthu uja wopunduka chibadwire kotero, anthu omvera aja sanakaikwa za ulaliki wamphamvu wa Petro panthawiyo kuti unalidi ulaliki wochokera kwa Mulungu. Pakhomo la kachisi lija pokhala “nthawi ya mapemphero” pankakhala anthu ochuluka kwambiri ngati momwe zimakhallira mu misika anthu akangolandira ndalama kumene. Anali malo ngati amene'wa omwe anasankhidwa ndi Mulungu kuti awonetsepo mphamvu zake ndi kulalika Uthenga Wake pochita chozizwitsachi. Moteronso, pa Machitidwe 5:12 timawerenganso kuti **“mwa manja a atumwi zizindikiro ndi zozizwitsa zambiri zinachitidwa mwa anthu”**. Izi ndi zosiyana kwambiri ndi ndondomeko ya Mzimu Woyera wa matcharitchi a masiku ano monga a Pentekositi; omwe amalimbikira kuti ali ndi Mzimu Woyera omwe mphamvu yake siimaonekera kweni kweni kwa anthu ena ayi koma kwa iwo wokha.

Tinenenso pano kuti ngati wolembe buku lino, kukambirana kwakukulu kunachitika ndi anthu ambiri omwe amanena kuti ali ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera, komanso kuona zomwe amatha kuchita zokhudzana ndi kudzozedwa ndi Mzimu Woyera. Ngakhale zimakhala choncho, palibe ndi tsiku limodzi lomwe pamene ndinakhutitsidwapo ndi zochitika za mtundu wotere; kenaka ndinayamba kumalingalira momwe Baibulo limafotokozera za Mzimu Woyera ndi Mphatso zake. Ndakhala nawo anzanga ambiri okhulupirira zimenezi koma analephera kundipatsa mfundo zokwanira zeni zeni zogwirizana ndi Mau Oyera pankhaniyi. Sindiye kuti sindimafuna kukhulupirira zomwe iwo amanena ayi, koma kuti ndimafunitsitsa kuti zizindikirozo zizigwirizana ndi Mau a Chiyeo. Kotero, ndichifukwa chake ndimamva chisoni anthu akamalimbikira zinthu zomwe zikusiyana kwathunthu ndi Mau Owuziridwa ndi Mulungu yemwe iwo amafuna kumupembedza. Machiritso ambiri omwe amati amachitika, samakhala owona ngakhale anthu akufa sangaukitsidwe monga zinaliri kale ndi anzathu aja. Tionenso mfundo yomweyi kuti Mulungu Iye Mwini, wakhala akuonetsa kwa anthu, omutsatira opatsidwa mphamvu yapadera ndi odzozedwa ndi Mzimu Wake wapadera. Mwaichi, ndikobvuta kwambiri kukhulupirira izi popeza *palibe “chionetsero cha Mzimu ndi Mphamvu yeni yeni”* pakati pathu monga zinaliri ndi akhristu oyambirira.

Ndikudziwa kuti ngakhale a Yuda mu chirunika choyamba, anatseka makutu awo pa zochitika ndi mphatso za Mzimu Woyera. Ankakayikira kuti Mulungu anawadzoza ndi Mzimu Woyera koma chifukwa panali chitsimikizo mu zochitika pamaso pawo, iwo anakhulupirira. Kotero, anabvomereza *“chifukwa munthu uyu achita zizindikiro zozizwitsa zambiri”* (Yohane 11:47) ndi *“...Pakutitu chawonekera kwa onse akukhala mu Yerusalemu...ndipo ichi sitingathe kukana..”* (Machitidwe 4:16). Momwemonso, onse omwe anamva akuphunzira akulankhula m'malirime *“anadabwa”* (Machitidwe 2:6). Zonse izi zikusiyana ndi zomwe zimachitika lero monga anzathu a Pentekositi amanenera. Ndizowonekeratu kuti Mzimu wa lero ndi ofookerapo poyerekeza ndi Mzimu wa nthawi imeneyo omwe unali Mzimu weni weni wa Mulungu. Ichi ndichifukwa chakuti anthu leroli amangoyerekeza chabe zomwe anzathu odzozedwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu kalelo anali kuchita. Choncho, sitinganene kuti lero anthu amalandiradi Mzimu Woyera chifukwa palibe umboni uliwonse m'machiritso, zozizwitsa ndi malirime awo zowonetsa kuti zimachokeradi kwa Mulungu. Machiritso ndi zozizwitsa zeni zeni zochokera kwa Mulungu zitachitika mu Mzinda wa Yerusalemu, sizingakhale zosiyana ndi zomwe zingachitike pa Trafalgar Square mu Mzinda wa London, kapenanso zomwe zachitika pa Nyahururu Park mu Mzinda wa Nairobi . Zonse zingadziwike mopanda kufunsapo mafunso okayikitsa popeza zawonekeratu kuti zochitikazo zatheka ndi Mphamvu yopambana ya Mzimu wa Mulungu. Ndipo kuti aliyense sangakayikire kuti lero Mzimu wa Mulungu ukugwiradi ntchito. Mosiyaniranatu ndi maonetsedwe a mphamvu ya Mulungu yotere mu matcharitchi a lero'wa, omwe amawuza dziko lonse kuti chikhulupiriro chawo chimagonera pa zinthu izi:-

- Kuchira (osati nthawi imodzi) ku zironda za m'mimba, ntchito ya machiritso imayamba nthawi zonse anthu akakumana kumapempherero.
- Anthu olumala amayamba kuwona pang'ono pang'ono, ngakhale kuti kenaka amadzakhalabe akhungu.
- Anthu omangika mu maganizo amamasulidwa
- Ofuna ntchito amayipeza , ndipo osauka amalemera komanso ofuna mabanja amawapeza mosabvuta - akamapemphera.

Mzitsanzo izi, tizindikire kuti kumapemphero otere, kumabwera anthu opunduka, odwala mu maambulasi ndi ena obwera okha ambiri. Koma zokhumudwitsa zimakhala zoti anthu onsewa amabwerera m'makwawo osathandizika konse. Zikanakhala kuti izi ndizotheka, sikukanakhala anthu odwala matenda ambiri ngakhale imfa imene padziko lino. Likanakhala dziko lokoma lopanda matenda kapena mabvuto ena ali onse kotero, tikanati Ufumu wa Mulungu watifikira. Tonse tikudziwa kuti izi siziri choncho ngakhale anzathu'wa amalengeza kwamphamvu za nkhani yotere. Ena amanena kuti anthu ambiri samachira chifukwa chosowa chikhulupiriro. Ife tikuti izi zikusiyana ndi Mau Opatulika popeza tikudziwa kuti kalelo anthu ankachira ngakhale akhale osakhulupirira iwo eni. Tizindikire kuti chikhulupiriro cha munthu ofuna chithandizo chimakhalapo mwa Mulungu wake kotero, ndichifukwa chake munthu uja amanyamuka kupita komwe kukuchitikira msonkhanoko. Munthu akasiyanitsa yekha zochitika pamalopo ndi zomwe amadziwa kuchokera mu Baibulo, ndi pamene amayamba kutaya mtima popeza wadziwonera yekha kuti zochitikazo sizikugwirizana ndi Mau a Mlengi wake. Tiona kuti chikhulupiriro chotsamira pa Mau ake ndicho chikhulupiriro cheni-cheni. Ngakhale nthawi ya Yesu, anthu ankachiritsidwa asanaonetse chikhulupiriro chawo. Umu ndi m'mene Mulungu ankaperekeramphatso yake ya machiritso. Munthu wina sanamudziwe Yesu koma anachiritsidwa (Yohane 5:13; 9:36).

Mapemphero amene akuchitika lerowa ndi chikonzero cha munthu kotero, n'chifukwa chake chikonzero chimenechi chimasiyana ndi ndondomeko ya Mulungu ndipo machiritso eni eni sangachitike m'njira imeneyi. Sichikonzero cha Yehova kuti ife tizingopita ku tcharitchi kukayimba ng'oma ndi zina zotero, kaya kukabvina ndi kuyimba m'manja osazindikira kapena kumudziwa Mulungu yemwe tikumuyimbira'yo ayi. Anthu atha kunena kuti akuchira chifukwa chonthunthumira ndi chilakolako chofuna kuchira koteronso, chikatha chilakolakocho, amabwerera kunyumba zawo monga momwe analiri poyamba. Mosiyana ndi izi, Petro anachiritsa kotheratu anthu omwe an'kagona mu ngalande ndi m'mphepete mwa misewu (Machitidwe 5:15); Machiritso mwa Mphamvu ya Mzimu Woyera omwe Paulo anachita, unali umboni waukulu ku nduna ya boma (Machitidwe 13:12,13), ngakhalenso kwa anthu achikunja ambiri amene ankakhala mu Mzinda wa Lysitra (Machitidwe 14:8-13). Zonsezi zin'kachitika mosalengeza ayi koma anthu ambiri an'kakhulupirira kwambiri chifukwa zonse zin'kagwirizana ndi cholinga komanso ndondomeko yake ya Chiuta. Mwaichi, anthu sanakayikire koma

kubvomereza atumwiwo kwathunthu kuti zochitikazo zinalidi zochokera kwa Mulungu.

Zotsatira za machiritso a Khristu nthawi zina zinali chimodzi modzi “...*kotero kuti anadabwa onse* (omwe anadziwonera okha), *nalemkeza Mulungu, nanena kuti, zotere sitinazione ndi kale lonse...*” (Marko 2:12).

MALIRIME

Akuphunzira ake a Yesu, ena a iwo asodzi a nsomba, ndi amene analandira udindo waukulu wopita kudziko kulikonse kukalalikira Uthenga Wabwino (Marko 16:15,16). Mwina nkhawa yawo yoyamba idali “...*koma ine sindidziwa zilankhulo zawo!*” Kwaiwo, sananenepo kuti “*sindinaphunzirepo zilankhulo zina*” chifukwa ngakhale ku sukuluko iwo sanapiteko mpang’ono pomwe, ndipo pokumbukira Mose m’chipululu kuti Mulungu adzalankhula ndi lirime lake mwa iye ngakhale anali wachibwibwi, iwo anadzipereka pa ntchito’yi. Timawerenga za iwo kuti “...*ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulukira...*” (Machitidwe 4:13). Ndipo ngakhale ophunzira kwambiri ngati Paulo, chilankhulo chidali chobvutabe mu dziko la eni, kotero, kunalidi kobvuta kulimbikitsana (maka podziwa kuti Chipangano Chatsopano kudalibe) mu chikhulupiro.

Pofuna kuthetsa bvuto limeneli la zilankhulo, Mulungu anatomiza Mzimu Woyera kuti anthuwo alandire mphatso ya malirime ndikuti azindikire cholankhulidwacho. Baibulo la N.I.V. limatanthawuzira liwu loti “malirime” kuti ndi “*zilankhulo*”. Tiona kuti pali kusiyana pakati pa cholinga cha Mulungu mu Baibulo potumiza malirime ndi momwe zimachitikira lero mu matcharitchi omwe amalankhula malirime. Chisokonezo chimenechi cha malirime chikhoza kutha pokhapokhapo ngati ife tingathe kuwerenga momvetsa bwino tanthawuzo leni leni lomwe lingapezeke mu Baibulo. Baibulo limafotokoza momveka bwino cholinga cheni cheni cha malirime nthawi imene ija ndinso tanthawuzo lake lomwe ndi “*zilankhulo za mu mayiko ena*”.

Nthawi ya mwambo wa Pentekositi, Yesu atangokwera kumene kupita kumwamba, akuphunzira ake a Yesu “...*anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera nayamba kulankhula ndi malirime ena,..unyinji wa anthu unasonkhana* (apa tionanso kuti zikuonetsa kwa khamu lonse cholinga cha

malirime), *nusokonezedwa popeza yense anawamva alikulankhula m'chilankhulo chake cha iye yekha. Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa sali Agalileya kodi? Ndipo nanga ife timva bwanji, yense mu chilankhulidwe chathu chimene tinabadwa nacho?...Aparti ndi Amedi, ndi Aelami,...tiwamva iwo alikulankhula mu malirime athu....Ndipo anadabwa onse, nathedwa nzeru*"; (Machitidwe 2:4-12). Zikuonekeratu kuti ndime zimenezi zikutsindika mobwereza mau oti *"anadabwa"* chifukwa chakuti chochitikacho panthawiyi chinali chinthu chachilendo kwambiri kwa anthu aja kotero, tionadi kuti ulaliki umene ulipo masiku ano pankhani ya malirime ukusiyana koposa ndi ndondomeko yomwe inachitika pa Pentekositi. Ngati chinthu chilichonse chichitika mu mphamvu ya Mulungu chimakhala cha mtengo wapatali, chozizwitsa popeza Iye ndi wamphamvu zodabwitsa ngati zinaonekera pa Pentekositi paja (Machitidwe 2); Koma ngati palibe Mphamvu ya Yehova, zonse zomwe zingachitike pamenepo sizimakhala zogwira mtima kweni kweni kwa anthu.

Anzanga nonse, tizindikire kuti mu Machitidwe 2:4-11, pali kusiyantsa matanthawuzo pakati pa liwu loti *"malirime"* ndi *"zilankhulo"*, ngakhale kuti mauwa amagwiritsidwa ntchito mofanana mu ndime zina za Chipangano Chatsopano. Mwachitsanzo mau oti *"anthu"*, *"mayiko"* ndi *"malirime"* amagwiritsidwa ntchito ngati liwu limodzi mu Chibvumbulutso 7:9; 10:11; 11:9; 13:7; 17:15. Komanso liwu loti *"malirime"* limagwiritsidwa ntchito potanthawuzira kuti ndi *"zilankhulo"* mu mabuku a Baibulo monga Genesis 10:5; Deuteronomo 28:49; Danieli 1:4.

Tingaonenso apa kuti 1 Akorinto 14 muli malamulo eni eni okhudza ntchito yangwiro ya Mzimu Woyera ndi malirime yomwe kwambiri inali kuyikirapo umboni pakati pa Ayuda; mu ndime 21 ya mutu womwewu, Paulo akuwakumbutsa anthu za Yesaya 28:11 za malirimewa pamene Yesaya analosera kuti anthu okhulupirira maka maka ophunzira ake a Yesu adzalankhula mu malirime polalika Uthenga Wabwino. *"...Kwalembedwa m'chilamulo, Ndi anthu a malirime ena ndipo ndi milomo ina ndidzalankhula nawo anthu awa;*". Tingaone kuti Yesaya 28:11 ananena za adani a ana a Israeli omwe adalankhulanso zilankhulo zachilendo pamene analowa kudzathira nkhondo mu dzikolo. Milomo ndi malirime tikatengera m'mene mauwa agwiritsidwira ntchito mu ndime imeneyi, akuonetsa kuti akuyimira zilankhulo zachilendo zakunja. Pali zionetsero zambiri zomwe tingazipezenso mu 1 Akorinto 14 zosonyeza kuti malirime akuyimira

zilankhulo zakunja zachilendo. Pongowerenga ndime zimenezi, tizindikiratu kuti malirime ndi milomo, cholinga chake chinali kuthandiza kufalitsa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndipo kuti atumwi aja ndi ena onse, ankalankhula zilankhulo zeni zeni zomwe eni zilankhulowo an'kazimva napindula. Kodi lero malirime akamalankhulidwa pakati pathu, alipo amamva napindula? Paulo mu ndime zimenezi akutsutsiratu bodza lomwe anthu ena an'kanena zokhudza mphatsozi mu mpingo kalelo, mwaichi, akutilangiza ndinsokutiphunzitsa mfundo zeni zeni ndi cholinga cha mphatso ya malirime ndi ulosi, kuti ife leronso tikhale ozindikira zimenezi ndipo kuti tikadziwa, tiphunzitse anzathu omwe samazindikira ichi kotero, nawonso apindulepo kanthu. Tiyeni tione ndemanga ya Paulo mwachidule mu 1 Akorinto 14:37:-

“Ngati wina ayesa kuti ali m'neneri, kapena wauzimu, azindikire kuti zimene ndilemba kwa inu ziri lamulo la Ambuye.”

Tadzimvera tokha tsopano kuti ngati wina amanena kuti ali ndi mphatsozi, ayenera alolere kubvomereza ndikuchita monga lamulo lokhudza mphatsozi limanenera mu Baibulo. Amene sabvomereza izi, ndiye kuti samadziwa, samafuna kumvera Mulungu komanso amakana kubvomereza kuti Baibulo ndilowuziridwa ndi mpweya wake. Onani ndime 11-17 (please check translation errors):-

“...Chifukwa chake, ngati sindidziwa mphamvu ya mauwo ndidzakhala kwa iye wakunja wonyoza ndipo wolankhulayo adzakhala mkunja wankhaza kwa ine...”

...Momwemo inunso, popeza muli ofunitsitsa mphamvu zauzimu, funani kuti mukachuluke mkumanga kwa mpingo.....

.....chifukwa chake wolankhula lirime, apemphere kuti amasulire... Pakuti ngati ndipemphera m'lirime, mzimu wanga upemphera, koma chidziwitso changa chikhala chosabala kanthu...

...Kuli kotani tsono? Ndidzapemphera ndi Mzimu, ndipo ndidzapempheranso mozindikira; ndidzayimba ndi Mzimu, koma ndidzayimbanso mozindikira.

...chifukwa ngati udalitsa ndi Mzimu, nanga iye wakukhala osaphunzira adzanena bwanji kuti Ameni, pakuyamika kwako, popeza sadziwa chimene unena?...

...Pakutitu iwe uyamika bwino, koma winayo sapindulapo.”

Kulankhula chilankhulo chomwe ena onse sakuchimva pamsonkhano wamapemphero sichinthu chanzeru chifukwa chakuti enawo samapindula chirichonse. Sikoyeneranso kunena kuti “Ameni!” pamene munthu sanamve chomwe chalalikiwa kapena chimene chanenedwa. Tiyenera tizindikire kuti munthu akati “Ameni!” zimatanthawuza kuti “zikhale choncho” mwachitsanzo, “ndibvomereza zonse zomwe zanenedwa mu pemphero limeneri”. Ndipo ndichifukwa chake Paulo akuti kulankhula chilankhulo chomwe abale ndi alongo athu sakutha kumva sindondomeko yabwino; Mphatso yotere sikuonetsa chikonzero cheni cheni cha Mulungu yemwe ndi Mwini mphatsoyo chifukwa palibe munthu amene angapindule pakati pa anthu omvera ndi olankhulawo. Apa zingatanthawuzidwense kuti cholinga cha mphatso ya malirime, machiritso ndi zozizwitsa ndi kufuna kupindulira anthu a chikhulupiriro ndi ena omwe angapezenso chikhulupiriro mwa Mulungu Mlengiyo. Tiona kuti izi ndi zosiyana ndi m'mene zikuyendera masiku ano chifukwa okhulupirira onse olankhula malirime lero, samamva zomwe amalankhula komanso omvera aja samamvanso koteru, malingana ndi Paulo, kulankhula malirime opanda tanthawuzo, chilankhulo chomwe wina aliyense sangamve, ziri chabe pamoyo wathu. Zonse zimakhala zopanda gawo pa chipulumutso cha munthu. Tafotokoza kale kuti cholinga cha buku lino ndi kuyesa yesa kutsimikizira anthu kuti ndondomeko ya Mau a Chiuta ndi yofunikira kuyitsata kwathunthu mosaphatikizapo komanso mosaganizira chikhalidwe china chonse chachikunja, ndipo mosafuna kuganizira za zilako lako zathu ayi.

Ndikumbukira tsiku lina a Billy Graham Crusade anapangitsa msonkhano wawo wa mapemphero. Ine ndinagawa timakalata topempha anthu omwe anapita kumsonkhanowo kuti palinso ndondomeko yabwino yomwe ingawathandize iwo kuti aphunzire ndi kuzindikira bwino Mau a Mulungu, potsata ndondomeko imeneyi. Maphunziro'wa ndi amene angawathandizenso iwo kukhala akhristu odzidalira ndi opindula komanso kuti, atha kuthandiza anzawo kudziwanso choonadi. Panali mayi wina yemwe ananditsimikizira kuti chikhulupiriro changa chomwe chiri cha abale mwa Yesu Khristu

(christadelphians) ndi chotsogozedwa ndi satana, yemwe kwa iye anati ndi mzimu oyipa. Kenaka anayamba kulankhula malirime mpaka panatha mphindi khumi. Ine ndi ena onse sitinathe kutolapo kanthu pa zimene ankalankhulazo! Apa tiona kuti ngati malirime aja anayenera kudzudzula ine ndi kuchenjeza ena amene anali pafupi ndi ine za chiphunzitso changacho kuti ndi choyipa, uthenga wotere sunafike kwa ine ndi ena onse aja! Kotero palibe amene anapindula kanthu. Izi zinandikumbutsa ndime 18 ya kalata ya Paulo kwa Akorinto mu 1 Akorinto 14:-

“...Ndiyamika Mulungu kuti ndilankhula malirime kuposa inu nonse”

Taonani anzanga, Paulo anayenera kulankhula malirime kwambiri chifukwa ankayenda yenda koposa, anazungulira dziko lonse lapansi kupambana wina aliyense pa nthawiyo choncho, kunali koyenera kwa iye kulankhula zilankhulo zosiyana siyana ngakhale sankazidziwa koma panthawi yolankhulayo ankamva ndikuzindikira chomwe ankalankhula:-

“...Koma mumpingo ndifuna kulankhula mau asanu ndi chidziwitso mozindikira kwanga (ndi inu) kutinso (mwaichi) ndikalangize ena, koposa kuti ndilankhule mau zikwi zikwi m'malirime osamveka” (please check translation!)

Anzanga muli apa, mukhoza kuoneratu kuti cholinga chinalipo pamene Mulungu anapereka mwayi wolankhula malirime mu ndime zimenezi. Kulalika za Yesu mu chiganizo chimodzi chomveka bwino kwa anthu, ndikofunikira kwambiri kusiyana ndi kutha nthawi yambiri popanda chopindulitsa kwa anthuwo, monga kulankhula m'malirime mopitiriza mphindi khumi koma pamene munthuyo sangatolepo kanthu. Apa zikuonetseratu kuti malirime a masiku ano sangakhale otsogoleredwa ndi cholinga cha Mulungu. Onani izi mu vesi 22 iri m'munsiyi:-

“Chotero, malirime akhala ngati chizindikiro, si kwa iwo akukhulupirira, koma kwa iwo osakhulupirira; koma kunenera sikuli kwa iwo osakhulupirira; koma kwa iwo amene akhulupirira...”

Ntchito ya malirime kotero, tiona kuti inali kulalika ndi kufalitsa Uthenga Wabwino. Pamene lero anthu amati, amalankhula malirime akakumana okhulupirira okha okha kapena nthawi zina munthu okhulupirira wa lero akamapemphera payekha. Sitinganene kuti uku ndi kukwaniritsa cholinga cha malirime opezeka m'Mau a Chiuta ayi popeza ndi zowonekeratu kuti palibe amene amapindulapo. Mwayi udapezeka ofalitsa Uthenga kwa anzathu a kum'mawa ku Ulaya mzaka za 1990. Takhala tikuona kuti makalata ofalitsira Uthengawu omwe ankgawidwa, analembedwa mu chingerezi pamene anthu oyenera kulandira Uthenga Wabwinowu samamva chingerezi. Tikhoza kuonanso apa kuti akanakhala kuti malirime akugwira ntchito, akanathandiza kwambiri pofalitsa Uthenga umenewu kwa anthu otere; Koma chifukwa chakuti sakugwira ntchito pakati pa anthu okhulupirira lero monga zinaliri panthawi yakale, izi sizingatheke kufalitsa Uthenga Wabwino mu njira yolankhula malirime. Kotero lero, anthu olankhula malirime amagwiritsa ntchito omasulira mzilankhulo zamayiko osiyana siyana akamalalikira mu mayikowo. Olankhula malirime a kale sankagwiritsa ntchito anthu omasulira chifukwa malirime kwa iwo kunali kulalikira kumene. Ndipo ndichifukwa chake:-

“...ngati mpingo wonse ukasonkhane pamodzi, ndi onse akalankhule malirime, ndipo akalowamo anthu osaphunzira kapena osakhulupirira, kodi sadzanena kuti mwayaluka?”

Izi ndi zimene zakhala zikuchitika. A chisilamu ngakhale ena a chikunja akhala akumaseka ndi kumanyogodola pamene zinthu zotere zikuchitika chifukwa sizimanyezimira cholinga cha Mulungu powona kuti anthuwo samatolapo kanthu. Kungomva zimene zimachitika mu mipingomo, ngakhale a khristu ena ambiri amadabwa ndi zochitikazo chifukwa ena amafika mpaka pomangodziririra tsiku ndi tsiku. Kodi tingati mphatso zakalezo zinayamba zafika pamene ziriri lerolino? Werengani vesi 27:

“...ngati wina alankhula lirime, achite ali awiri, koma oposa atatu iai, ndipo motsatana; ndipo m'modzi amasulire.”

Mau a Mulungu akuti awiri kapena osaposeera atatu mu mpingo wonse uja atha kulankhula mu malirime mapemphero kapena ulaliki ukamachitika. Sipayenera kukhala anthu opitirira nambala imeneyi pamene anthu alankhula mu malirime mu mpingo pa ulaliki wina uliwonse. Apa zikutanthawuza kuti

ngati pamsonkhano wa mu mzinda wa London, olalika atha kulalikira mu chingelezi, ndipo ngati kuli a Chewa, ma German, French etc; Chiganizo chirichonse chonedwa, chizimasuliridwa mzilankhulo zimenezi. Zonse zingayende motere:-

Mlaliki :	Good morning
Omasulira Woyamba:	Moni nonse (Chichewa)
Omasulira Wachiwiri:	Guten a bend (chi German)
Omasulira Wachitatu:	Bon soir (chi French) etc

Paulo akuti ndondomeko yake ndiyo kulankhula motsatana komanso motsogozedwa ndi Mzimu Woyera osati mwachisokonezo ayi koma ndithu m'chilongosoko cha chifuniro cha Mulungu. Zikatero, sipakhala mtsogolero ndi olamulira monga tionera lero ayi popeza amatsogolera ndi Mwini Wake Mulungu koteru, cholinga chake zonse zikakwaniritsidwe.

Mphatso ya Mzimu Woyera ya malirime, iyenera kugwira ntchito mogwirizana ndi ulosi koteru, Uthenga Owuziridwa ukathe kumveka mu malirime omwe ndi zilankhulo zachilendo kwa m'neneriyo. Chitsanzo chimodzi cha zinthu zoterezi zomwe zikugwira ntchito pamodzi, tingawerenge pa Machitidwe 19:6. Tiyerekeze kuti Mlaliki wa mu Mzinda wa London uja akulalikira mu chi French, ndiye kuti ngati ambiri ndi a chi French, omasulira aja akhala m' Chichewa, Chingerezi ndi chi German ndipo zonse zizichitika motsogozedwa komanso mowuziridwa ndi Mwini Wake Chiuta. Mphatso ya malirimeyi in'kathandiza kuti anthu onse adzimvere okha Uthenga Wabwino womwe Mulungu wafuna kuti ulalidwe panthawi yopatulidwayo. Tionanso kuti ngati Mlaliki uja afunsidwa mfuso mu chi Frenchi, ngati akulalika m'chi Frenchicho, sangathe kuyankha chifukwa iye saadziwa kulankhula chi French. Mwaichi, mphatso yomweyi inkathanso momasulira momwemo kuthetsa bvuto lotere.

Popanda mphatso ya mamasulidwe a malirime mkati mwa malirime momwemo, sizikanakhala zotheka kugwiritsa ntchito malirime moyenera panthawi imene ija “...ndipo m'modzi amasulire. **Koma ngati palibe omasulira, akhale chete mu mpingo...**” (1 Akorinto 14:27,28). Kulankhula

malirime opanda omasulira ndi ndondomeko yeni yeni ya Mulungu, ndikulakwa komanso kusamvera malamulo a Mulungu. La la la la la la la, sichilankhulo china chirichonse chamatanhawuzo pa dziko lapansi. Onani ndime 32, 33:-

“...ndipo mizimu ya aneneri imvera; pakuti Mulungu saali Mulungu wa chisokonezo ayi koma wantendere; monga mwa mipingo yonse ya oyera mtima...”

Kukhala ndi mphatso ya Mzimu kotero sikutanthawuza kuti munthu amaumirizidwa kuchita zinthu ndi kukhala osaganiza chifukwa cha Mzimuwo ayi, koma kuti pali nthawi ina Mzimu uja umamutsogolera ndi kumuunikira munthu uja ikafika nthawi yoti cholinga cha Mulungu chikwaniritsidwe. Ena amanena kuti mizimu yoipa imalowa mu mitima mwa anthu osakhulupirira ndikuti anthu okhulupirira amadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Koma tikaona Mphamvu ya Mzimu Woyera mu 1 Akorinto 14:32 unali ndi gawo mu udindo wa munthu odzozedwayo kuti akakwaniritse komalizako. Siudali ndipo siuli mzimu wotsutsana ndi Mzimu wabwino lero mwa munthu ayi. Taonetsa kale kuti Mzimu Woyera unkapatsidwa kwa anthu kuti ntchito yopatulidwa mwapadera igwirike ndiponso kuti ntchitoyo ikagwiridwa Mzimuwo umachotsedwa mwa munthuyo, samakhala nawonso ayi.

Ngakhale Paulo anayesetsa kuwapempha anthu kuti asamanamizire kuti ali ndi Mzimu Woyera, komanso kuti Mphatso za Mzimu Woyera zimayenera kugwiritsidwa ntchito mogwirizana ndi cholinga cha Namalenga, anthu a lero mu mipingo yamakono samamva kokwanira ayi (ndime 33).

“...Akazi akhale chete mu Mipingo. Pakuti sikuloledwa kwa iwo kulankhula. Koma akhale omvera, monganso chilankhulo chinena...” (Vesi 34).

Malamulo akuti ngakhale mkazi akhale ndi mphatso zimenezi, sayenera kuzigwiritsa ntchito mu tcharitchi nthawi ya mapemphero. Anthu sayenera kuchita zinthu chifukwa chongonthunthumira chabe ayi, kutsata lamulo ndi cholinga cha Mulungu pa zinthu zopatulidwa mwapadera ngati zimenezi. Kotero, malirime ayenera kukhala ndi tanthawuzo kwa ana, amuna ngakhalenso azimayi mu mipingo mwathu.

Timadziwa kuti akazi ndi ana ndiomwe amachuluka mu mipingo ya makono polankhula malirime kwambiri koma izi, sizikugwirizana ndi chilongosoko cha Mau a Mulungu mu ndondomeko yeni yeni ya malirime. Ena amati Paulo sankakonda akazi, komanso kuti chikhalidwe cha chi Yuda sichin'kalola azimayi kukhala ofanana ndi abambo kotero, Baibulo limakamba zomwe a Yuda an'katsata; Tiyeni anzanga titsate zomwe Mau owuziridwa ndi Mulungu amatilangiza ife kuchita zomwe Mulungu afuna ife tichite, osati tichite chifukwa chakuti tifanane ndi zomwe anzathu amakhulupirira ayi:- **“...Ngati wina ayesa kuti ali m'neneri, kapena wauzimu, azindikire kuti zimene ndilemba kwainu ziri lamulo la Mulungu Ambuye”** (1 Akorinto 14:37) osati lamulo la Paulo ayi!

Wokhulupirira aliyese wa Baibulo, kuti ndilowuziridwa, kotero, ayenera kudziwa kuti mau a Paulo mu 1 Akorinto 14:37 ndi owuziridwa ndipo ayenera kuwamvera ndikuchita monga Mauwo atilangiza. Pokha pokha ngati sitikhulupirira ndipo tiri ndi baibulo lina losiyana ndi Mau ake, iyo ndi njira ina, ndipo kutero ndi chinthu choopsa kwambiri kwa munthu yemwe anasankha kudziwika ndi dzina la Khristu (anadzitchula dzinali pa tsiku la ubatizo wake).

Ndipo ngati ndi mpingo womwe umanena ichi, kodi tingati ndi mpingo wa Mulungu? Nanga ife ngati olakalaka kuchita chiyero cha Baibulo lowuziridwalo tikhala bwanji mu mpingo wosakhulupirira Mau Oyera a Mulungu ngati umenewu?

2.4 KUCHOTSEDWA KWA MPHATSO

Mphatso zozizwitsa za Mzimu wa Mulungu zidzagwiritsidwanso ntchito ndi okhulupirira pamene dziko lapansi lidzasinthidwa kukhala mu ulemere wa Ufumu wa Mulungu ndipo apa ndi pamene Yesu Khristu adzabwerenso. Mphatso zimenezi ndi zomwe zikutchedwa **“...Mphamvu ya nthawi irinkudza...”** (A Hebrai 6:4,5); ndipo Yoweli 2:26-29 akufotokoza za kutsanulidwa kwa mphatso za Mzimu, ana a Israeli akadzalapa. Tikamvetsetsa kuti Mphamvu za Mzimu zimenezi zidzaperekedwanso kwa okhulupirira Yesu akadzabwera, ndi chitsimikizo chokwanira kuti lero Mzimuwo sukugwiranso ntchito ayi; udzachita kubwera kwa okhulupirira! Apa tiyenera kuona kuti

zizindikiro zakubweranso kwa Khristu zikukwaniritsidwa padziko lapani munga timawerenga mu Mau ake (onani malozero [appendix 3] achitatu).

Tiri ndi maulosi okwanira ndinso omveka bwino mu Baibulo owonetsa kuti pakati pa chirumika choyamba pamene mphatso za Mzimu zinalipo, ndi pano pamene tikuyembekezera kubweranso kwa Ambuye kachiwiri, kuti ndithu zowona, mphatso za Mzimu zinachotsedwa pakati pathu:-

“...koma ngati pali zonenera (ulosi) zidzakhala chabe, kapena malirime adzakhala chabe, kapena nzeru idzakhala chabe. Pakuti ife tidziwa mdera mdera (in part?[mosakwanira]), chifukwa tinenera (tilosera) mdera mdera (in part?). Koma pamene changwiro chafika, tsono chamdera mdera (incomplete or in part?) chidzakhala chabe”
(1 Akorinto 13:8-10).

Monga tawerenga, tiona kuti Mphatso za Mzimu m'chirumika choyamba zidayenera kuchotsedwa popeza “...**pamene changwiro chafika** (chomwe ndi Baibulo), **tsono cha mdera mdera chidzakhala chabe**”. Kufika kwa changwiro sikungakhale kubwera kwa Khristu popeza tawona kale m'mwambamu kuti Yesu akadzabweranso, Mphatso za Mzimu Woyera zidzaperekedwanso kwa okhulupirira onse; mwachitsanzo, onse okhulupirira adzakhala ana a Mulungu, adzakhala ngati Khristu! Apa tionanso kuti liwu limene linamasuliridwa kuti “**changwiro**” mu chi Greek, likuyimira chomwe chiri “**chodzala**” kapenanso kuti chomwe chiri “**chomalizidwa**”. Choncho, apa ungwiro sikumasulira koyenera kweni kweni kwa liwuli kotero, changwiro sichikuyimira choyera chifukwa sizikugwirizana ndi mavesi oyambirawo.

Kotero tinganenenso kuti ngakhale kusakwanira kwa nzeru kukhala chabe popeza tsopano anthu ali ndi nzeru zokwanira zowathandiza kudziwa zambiri za Mau ake kuchokera m'Baibulo. Chifukwa chake ndi chakuti nzeru'zo anaazipeza popeza panaali maulosi ndi mphatso za malirime zomwe lero zatipatsa Baibulo ngakhale kuti maulosi ndi mphatso'zo zinachotsedwa pakati pathu. Mulungu an'kalankhula zakutsogolo m'maulosi ndi malirime amenewa zomwe zinalembedwa mowuziridwa ndi Mzimu wake.

M'chirumika choyamba, okhulupirira aliyense ankatha kumva za maulosi kuchokera kwa akulu akulu a mpingo zokhudza kayendetsedwe ndi chikhalidwe choyenera mu mpingo; ankatha kudziwa magawo ochepa

kwambiri okhudza moyo wa Yesu Khristu; Mwina anaamvaponso kuwerengedwa kwa makalata awiri kapena atatu a Paulo m' masunagoge. Koma pamene maulosi, malirime ndi zozizwitsa zonse zinalembedwa ndi kutumizidwa ku mayiko onse padziko lapansi, palibe chifukwa chakuti pakhalenso maulosi, mphatso za malirime ndi zozizwitsa popeza zonse zalembedwa ndipo ndi zodzaza komanso zokwanira pamoyo wathu wachiyero. Kotero, mphatso za Mzimu zinakwaniritsa ndi kudzadzitsa Chipangano Chatsopano:-

“...Lemba lirilonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsitsimutso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha mchilungamo: Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iriyonse yabwino (to become “perfect?”) (2 Timoteo 3:16,17).

Ichi ndi chomwe chikhala chokwanira (cholungama?) kapena chodzaza ndi ***“Mau Oyera”***; Kotero ngati ***“Mau Oyera”*** anali owuziridwa ndipo analembedwa, ndiye kuti ***“...Cholungama, chodzaza ndi chokwanira”*** chabwera kwaife (kapena tinene kuti chinabwera kwaife) mwaichi, mphatso za Mzimu zinachotsedwa pakati pathu ndipo ziyenera kuteru.

Tikawerenga Aefeso 4:8-14 atitsimikizira polumikiza mfundo imeneyi yoti ife lero ndife okwanira:-

“...Mmene anakwera kumwamba, Ndipo Iye anapatsa Mphatso kwa ena kukonzera ndi kumangirira thupi la Khristu; kufikira ife tonse titafika ku umodzi wa chikhulupiriro (monga chikhulupiriro chimodzi chokha) ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro (wachikwane).....Kuti tisakhalenso makanda, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya chipulumutso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kukatsata chinyengo cha kusokeretsa;”

Mphatso za m'chirumika choyamba zin'kaperekedwa mpaka pamene munthu wangwiro ndi wodzala bwino anapangidwa powerenga ndi kumva Mau a Mulungu a Chiyero, ndipo 2 Timoteo 3:16,17 akunena kuti ***“...munthu wa Mulungu akhale wangwiro*** (wokwanira)” polola mlozo ndi malangizo a ***“...Lemba lirilonse”***. Akolose 1:28 akutiphunzitsanso kuti ***“Ungwiro”***

umabwera ngati munthu amvera Mau a Mulungu. Munthu akamvetsetsa Mau a Chiyero cha Mulungu, sangadabwe kwambiri kuona kuti lero kuli ziphunzitso zambiri mu mipingo yosiyana siyana pakati pathu. Koma tikaonetsetsa, tiona kuti pali Baibulo limodzi lokha, ndipo monga **“mau anu ndi choonadi”** (Yohane 17:17), tikaphunzira ndime zake modzipereka ndi kuzindikira, tidzapeza **“...umodzi wa chikhulupiriro”** chomwe chikambidwa pa Aefeso 4:13. A Khristu eni eni owona kotero, ali wodzaza, wokwanira ndi angwiro chifukwa cha **“...pamene changwiro chafika...”** Kapena titi chodzazidwa, chokwanira, cholembedwa, Mau okwanira ndi odzaza a Mulungu. Mau awa ndi okwanira mu uneneri, ulosi, malirime ndi mu zozizwitsa zonse zimene zingakhalepo!

Mukawerenga mofatsa, muzindikira kuti Aefeso 4:14 akufananiza Mphatso zozizwitsa za Mzimu ngati khanda la mwana mu Mau Oyera, ndipo ma Ulosi, akufotokozanso za momwe Mphatso zozizwitsazo zinachotsedwera pakati pa okhulupirira. 1 Akorinto 13:11 akunena chimodzi modzi. Apa tsopano, sikulakwa kunena kuti yense yemwe amanena kuti analandira Mzimu Woyera lero, ndi kuti, ali ndi Mphatso za Mzimu Woyera, ndi osakhwima mu chipembedzo ndipo samazindikira chipulumutso cheni cheni ndi cholinga cheni cheni cha Mulungu Yehova. Choyenera kuchita kwa ophunzira onse a Mau a Mulungu ndi kumvetsa, motsata ndondomeko yake kotero, anthu otsata izi adzasangalala pozindikiranso kuti tsopano ali okwanira, a changu ndi angwiro mu nzeru zake za Yehova zomwe waziulula kwaife, kuti ifeyo tikamvere podzichepetsa ndi ulemu kwa Iye.

MALANDIRIDWE A MZIMU LERO

Pomaliza, tinenepo kuti onse omwe amaganiza kuti ali ndi Mphatso ya Mzimu Woyera lerolino:-

- **“...Kulankhula mu malirime...”** lero kumatanthawuza kubwereza mau amodzi modzi kawiri kawiri monga **“Lala, lala, lala, shama, shama, shama; Khristu, Yesu, Yesu,.....” etc.** Tifuna tinene pano kuti mau otere satanthawuza chirichonse mu zilankhulo zathu padziko lonse lapansi. Monga tanena kale, m’malirime eni eni a Mzimu, anthu amatha kumva zonse zomwe zikulankhulidwazo mopanda kukayikira popeza ndi chilankhulo cheni cheni cha anthu ndipo kuti munthuyo, an’kanena za utumiki ndi zolinga za Mulungu panthawiyo. Ngakhale ena sanathe

kumva, komabe Uthengawu umamveka kwa anthu ena omwe Mulungu wafuna kuti amve mu chilankhulo chawo nthawi imeneyo. Tiona kuti izi siziri choncho ndi malirime a masiku ano, zomwe zimaonetseratu kuti malirime otere, samagwirizana ndipo sakupereka chikhulupiriro kapena ungwiro weni weni okwanira wa Mulungu zomwenso zinali zolinga za Mphatso'zo m'chirumika choyamba chija.

- Ena mwa anzathu a Pentekositi amati malirime ndi chizindikiro chowonetsa “...*kupulumutsidwa...*” kotero aliyense wopulumutsidwa ndi wotembenuka mtima ayenera alankhule malirime. Makambidwe otere ndi osagwirizana ndi chiphunzitsa cholondola cha Baibulo ndi mpingo woyamba, omwe umatiphunzitsa kuti onse omwe anali okhulupirira analandira mphatso za Mzimu zosiyana siyana, anapanga thupi limodzi la mpingo. Siyense amene anali dzanja kapena mwendo, kotero, siyense amene anali ndi Mphatso monga ya malirime, kapena ya machiritso. Kusiyana kwa Mphatso kun'kayimira (kapena titi kukuyimira) ziwalo zosiyana siyana za thupi limodzi lomwelo limene liri chiphiphiritso cha mpingo! Mau a Mulungu otere ndiwo chipulumutso chowona; tisakhale ndi mtima wolalika mau a mu mtima mwathu. 1 Akorinto 12:17, 27-30 titha kuwerenga izi momveka bwino:-

“...Ngati thupi lonse likadakhala diso, kumva kukadakhala kuti? Ngati thupi lonse likadakhala khutu, kukadakhala kuti kununkhiza?....Koma inu ndinu thupi la Khristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. Ndipotu Mulungu anayika mu Eklesia, poyamba atumwi, achiwiri aneneri, achitatu aphunzitsi, kenaka zozizwitsa, pomwepo Mphatso za machiritso, mathandizo, maweruziro (Government?), malirime amitundu mitundu. Kodi ali onse achita zozizwitsa? Ali nazo Mphatso za machiritso onse kodi? Kodi onse alankhula ndi malirime? Kodi onse amasulira Mau?”

Mfundo yomweyi inakambidwanso koyambirira kwa gawo limeneri:-

“...Pakuti kwa m'modzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa m'zake mau a chidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: Kwa wina chikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za machiritso, mwa Mzimu m'modzi'yo; ndi kwa wina machitidwe a mphamvu; ndi kwa wina chinenero; ndi kwa wina chizindikiro cha mizimu; kwa wina malirime a mitundu”

mitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malirime. Koma zonse izi achita Mzimu m'modzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. Pakuti monga thupi liri limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse zathupilo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi; momwemonso Khristu.” (1 Akorinto 12:8-12).

Tonse ngati a khristu eni eni sityenera kunyozera mfundo yotere podziwa kuti ndiye Mau eni eni a Mulungu ochokera m'Buku lake.

Bvuto lina la anzathu amene amati amalandira Mzimu Woyera ndi pamene tiganiza za Filipino yemwe anatembenuza anthu ambiri mu Mzinda wa Samaria – mwachitsanzo, an'kabatiza m'madzi anthu ambiri pokha pokha akazindikira ndi kudziwa bwino Uthenga Wabwino, koma sanalandire Mphatso za Mzimu; chifukwa timva kuti atabatizidwa anthuwo, Petro ndi Yohane anabwera kwaiwo: *“Ndipo Filipino anatsikira ku mudzi wa ku Samariya, nawalalikira iwo Khristu.....anabatizidwa ambiri amuna ndi akazi,...amenewo, m'mene adatsikirako, anawapempherera, kuti alandire Mzimu Woyera: Pakuti kufikira pamene n'kuti asanagwe pa wina m'modzi wa iwo; koma anangobatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu. Pamenepo anayika manja pa iwo, ndipo analandira Mzimu Woyera. ...Koma Simoni pakuona kuti mwa kuika manja a atumwi anapatsidwa Mzimu Woyera,...”* (Machitidwe 8:4-8). Tikhoza kuwona kuti kupatsidwa kwa Mphatso ndi Mzimu Woyera kun'katheka mwakuyika manja a atumwi aja pa iwo okhulupirirawo, izi ndi zinthu zomwe lero sizichitika ndi anzathu omwe amati ali ndi Mzimu Woyera.

A Pentekositi ena amati malirime sichizindikiro chokwanira chowonetsa kuti munthu ndi opulumutsidwa. Izi zikungosonyezzeratu kuti pali kusiyana kwakulu pa chikhulupiriro pakati pa anthu omwe amati ali ndi Mphatso za Mzimu Woyera ngakhale kuti akugwiritsa ntchito Baibulo limodzi lomwelo. Munjira yomweyinsu, ena mwa anthu amenewa amakhulupiriranso kuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa pansu pompano pamene ena mwa iwo amati Ufumu wa Mulungu uli kumwamba. A katolika amakhulupirira kuti Mzimu Woyera umawauza zoti ayenera kupembedza Maria ndi Papa, pamene a Pentekositi ena amatinso Mzimu Woyera umawalamula kuti sayenera kulambira Papa chifukwa ndi odana ndi chipembedzo cha Khristu kotero, sayenera kulemekeza chipembedzo cha a katolika. Pamene Yesu Mwini, anati yense wolandira *“mpumuzi”* (nkhoswe?), *“yemwe ndi Mzimu Woyera”*, adzatsogoleredwa *“.....m'choonadi chonse;.....patsiku limenero*

(mudzayenera) *simudzandifunsa kanthu.....Mpumuzi ndi mtetezi.....adzakuphunzitsani inu zinthu zonse, ndipo adzabweretsa zinthu zonse kuti inu mukakumbukire zonse ndidazinena ine...*” (Yohane 16:13,23; 4:26).

Apa tiphunzira kuti, sipayenera kusiyana maganizo ndi chikhulupiriro pakati pa okhulupirira Mphatso za Mzimu Woyera chifukwa Mulungu ndi m’modzi komanso Mzimu ndi umodzi omwewo; ndipo zonse zochitika ndi okhulupirira zonsezi zimachokera m’Mau ake a Yehova omwewo; ngati lero pali zikhulupiriro zosiyana siyana ndi chifukwa chakuti anthu amafuna kulowetsa tchimo mu chipembedzo poyikamo Mau awo, omwe ndi ogwirizana ndi zolinga zawo zomwe tsopano zimasiyananso pakati pawo. Anthu ayenera kutsogoleredwa ndi Mau ake popeza Mauwo ndi owuziridwa ndi Mulungu wa ndondomeko osati wa chisokonezo ayi.

“Kufunikira kolankhula malirime mwa anthu ena osamvetsa bwino sikumagwirizana ndi m’mene Baibulo limafotokozera. Ndongomeko ya Mphatso za Mzimu mu Aefeso 4:11 sizikambidwa zomwe anthu otere amanena kotero, ngakhale mu 1 Akorinto 12:28-30. Tikudziwanso kuti mu Chipangano Chatsopano Mphatso ya Mzimu inagwiritsidwa ntchito katatu kokha (Machitidwe 2:4; 10:46; 19:6).

Titero kuti malirime ndi zozizwitsa za anzathu a lero, ziyenera kuyesedwa ndi mlingo wolembedwa mu Baibulo chifukwa ndiye Mau owuziridwa ndi Yehova monga taonera mu phunziro lino pa za ntchito ya Mzimu wa Mulungu. Mwaichi, tikunenetsa kuti chirichonse chochitika mosiyana ndi chilongosoko cha Mau a Chiuta m’malirime, machiritso ndi zozizwitsa za lero sizochokera kwa Mulungu ayi, kotero, zilibe gawo lina lirilonse pa chipulumutso cha munthu ndipo sizingakhale ntchito za Mzimu Woyera. Yense payekha, yemwe amati ali ndi Mzimu Woyera lero ayenera kufufuza kwambiri m’Baibulo zoonza zeni zeni za ntchito yaikulu ya Mzimu’wo pa chipulumutso. Tionanso kuti ali ndi ntchito yayikulu koposa, kuti ayankhe mafunso okhudza Buku Loyera pankhaniyi kotero, ntchito zakezo zikagwirizane ndi ndondomeko ya Baibulo. Sitiyenera kukhala ndi chipembedzo chochita zinthu zosiyana ndi zolembedwa mu Buku Lopatulika ayi koma kuti Mau akewo akhale m’tsogoleri ndi muuni wa moyo wathu padziko lino.

Tiyenera kuzindikira kuti machiritso ndi malirime akhoza kuchitika mosagwirizana ndi Mphamvu ya Mulungu ndipo izi zimasiyana kwambiri ndi chilongosoko cha Buku Loyer. Leronso izi zikuchitika pakati pa anthu padziko lapansi.

Timamva kuti anthu amagwiritsa ntchito kagawo kochepe zedi ka ubongo wawo popanga zinthu zosiyana siyana monga anzathu a zofufuza fufuza amanenera. Amanenanso kuti maganizo paokha amatha kumuondetsa munthu, maganizo amathanso kulamulira zonse zochitika mthupi la munthuyo monga kayendedwe ka magazi ndi zina zotere: moteronso, angathenso kumulamula munthu kukhulupirira kuti moto sungamuotche. Anzathu a chi Hindu amachita izi mwina chifukwa cha mankhwala kaya pongokhulupirira chabe koma zakhala zikuchitika. Munthu akamanthunthumira kuti chinthu china chimuchitikire, iye atha kuchita zinthu zazikulu pogwiritsa ntchito gawo lalikulu la ubongo wake mosiyana ndi momwe timachitira nthawi zonse, chitsanzo;- kuthamanga kwambiri paminga pamene munthu akuthawa mkango koma osabvulala! Kudulidwa mikono kapena miyendo koma osamva ululu mpaka pamene munthu afika ku chipatala! Zonsezi mukhoza kubvomereza kuti zakhala zikuchitika pakati pathu. Tiona kuti apa munthu amagwiritsa ntchito ubongo wake mokwanira panthawi imeneyi mongoganizira kuti sanabvulale pamene wabvulala. Zinthu zotere zimachitikanso pamene munthu wadzidzimuka kapena wanthunthumira pa chinthu china chake kuti chimuchitikire chifukwa iye wachifunitsitsa. Chitsanzo china ndi za anzathu a nsayansi, amatha kuganiza ndi kupanga ndege, sitima, makina a kompiyuta zomwe ndi zofanana kwambiri ndi zinthu za chilengedwe. Ndipo n'chifukwa chake panthawi ya machiritso ndi zozizwa za masiku ano, anthu angaganize kuti achiritsidwa koma zomvetsa chisoni kuti akangochoka, amabwereranso mwakale ngati momwe munthu obvulala uja amamvera kupweteka pakapita nthawi yochepa. Mwanjira iyi, tikuona kuti machiritso a mtundu otere, simachiritso ochokera m'Mphamvu ya Ambuye Wathu Yesu Khristu. Tiyenera kukhala a tcheru ndi ziphunzitsa za mtundu umenewu pofufuza ndi kutsamira pa Mau a Mulungu kuti tisasokere.

Machiritso, malirime ndi zozizwitsa zizichitika osati chifukwa chakuti tiri ndi mtsogoleri kapena nyimbo yapadera yoyambira izi ayi, koma kuti anthu adzazidwadi ndi Mphatso za Mzimu. Yesu, Petro, Paulo onse analibe utsogoleri wa m'kachisi kapena nyimbo zothandiza kuti akhale ndi Mzimu wa Mulungu; Koteru, Mphamvu ya Mzimu inkabwera pakakhala chinthu

chofunikira kuti mphamvu ya Mulungu iwonekere pamaso pa anthuwo. Mphamvuyi siinkabwera chifukwa chakuti pali nyimbo kaya m'tsogoleri wina aliyense ayi koma chifukwa chakuti, Mulungu akufuna kukwaniritsa cholinga chake panthawi yokhayo. Lero anthu mu tcharitchi, amakonzekera kuti tsopano yakwana nthawi yolandira Mzimu, malirime ndi machiritso chifukwa chakuti m'tsogoleri wayambitsa nyimbo; izi sizogwirizana ndi chikonzero kapena cholinga cha Chiuta ndipo ziribe tanhawuzo m'moyo wathu wa chi khristu maka maka pamene zikusiyana kwambiri ndi chilongosoko cha Baibulo. Tiwona kuti ngakhale a khristu a magulu ena amatha kunenanso kuti ali ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera koma yosiyana ndi magulu ena a chi khristu anzawo. Tiyenera kuzindikira kuti Mulungu m'modziyo, sangapereke ndondomeko yotsutsana ya malirime, machiritso ndi zozizwitsa kwa a khristu omwense amakhulupirira chipulumutso chosiyana ndi Baibulo lomwe ndi Mau ake. A khristu ena amafanana ndi a chisilamu mu zikhulupiriro zawo za mtundu womwewu wa Mphatso za Mzimu. Tonse tikudziwa kuti cholinga cha mphatso za Mzimu Woyera mu chirumika choyamba chinali kuwonetsa kwa anthu kuti chi khristu ndicho chipembedzo cheni cheni pamaso pa Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu; Ndipo kuti ndi chosiyana kwambiri ndi zipembedzo zina zonse. Ngati mphatso za Mzimu Woyera lero zifanana ndi zozizwitsa za zipembedzo zina, zikuwonetseratu kuti ndi zosachokera kwa Mulungu maka maka pamene zikusiyana koposa ndi chilongosoko cha Ambuye Yehova Mulungu Wathu. Tiyeneranso kuyesa machiritso ndi zozizwitsa za masiku ano polingalira zomwe zinalembedwa mu Baibulo popeza ndiwo mlingo weni weni wokwanira wa Mulungu. Tikatero, tidzawona tokha kuti ndi zowona Mphatso za Mzimu za m'chirumika choyamba lero kulibe, zinachotsedwa monga timawerenga pa 1 Akorinto 13:8-9.

Mongopereka chitsanzo cha ena mwa magulu omwe amati ali ndi Mphatso za Mzimu Woyera lero munjira imeneyi, ndi m'modzi wa okhulupirira wa Pentekositi bambo William Campbell yemwe anayambitsa "Mpingo wa a Khristu" mu chaka cha 1967. Bambo Campbell anawonetsera poyera kwa anthu pomanena kuti zipembedzo zonse za chikunja ndi a khristu ena, ali ndi malirime koma akuti amalankhulidwa mosiyana. Kotero, chitsanzo cha mulungu wa chikunja wa mtundu wotere ndi ansembe a chipembedzo cha "Oro" kudziko la Kuwait, omwe akuti amaonetsa mphamvu zake mu maphokoso a mau osiyana siyana omwense amatha kumasulidwa ndi ansembewo. Tiwona kuti zinthu ngati zimenezi zimachitikanso pakati pa mipingo yina ya Pentekositi kapena magulu ena a chikhristu. Tizindikirenso

kuti mamasulidwe a malirime eni eni kalelo an'kathanso kuchitika ndi anthu ena osakhulupirira osati a nsembe okha okha ayi.

Lero a chisilamu, akhala akugonjetsa akhristu ambiri m'nkhondo zomwe zakhala zikuchitika m'mayiko a ku Afrika ndipo izi sizikanatheka zikadakhala kuti mphatso za Mzimu ziripobe mwa akhristu'wo monga zidaliri kale. Timawerenga pa Yohane 14:12,16 kuti onse amene adzalandire Mphatso ndi "mpumuzi (nkhoswe?)" wa Mzimu Woyera m'chowonadi, adzachita zazikulu zoposa izi; (zoposa zomwe Yesu anachita). Akhristu ena amati izi zidzachitika kwa yekhayo yemwe ali ndi chikhulupiriro. Tikudziwa kuti zonsezi ndi zowonadi, koma sizitanthawuza kuti iwo ali ndi chikhulupiriro choposa ena onse omwe sangathe kuonetsa mphatso za Mzimuzo chifukwa chakuti tikudziwa, sachita "zazikulu zoposa" zomwe Yesu Khristu anachita (Yohane 14:12). Apa Yesu sakunena kuti akhoza ayi koma kuti "adzachita zazikulu zoposa izi ndipo izi ziyenera kudzachitika motsata ndondomeko yeni yeni ya Baibulo!"

2.5 BAIBULO LAMULO LOKHALO

Pa zimene tawona pakali pano, taphunzira kuti Mzimu wa Mulungu ndiye maganizo ake ndi cholinga chake, komanso kuti ndi Mphamvu zake zomwe amatha kupangira zinthu ndi ntchito zake zonse. Tatsimikiza pa mfundo yoti Mzimu Wake unawululidwa mu Mau ake Opatulika. Ndipo tawonanso kuti chisokonezo chinabwera kapena kuti chikubwera chifukwa anthu sadafune kuzindikira bwino ndi kumvetsetsa modekha Mau Oyera pokhudza nkhani yotere kotero, sitingathe kunyadira Mau a Mulungu mu chowonadi. Popeza ndi kobvuta kumva mozindikira kuti Mphamvu yayikulu yotere idaperekedwa mu Buku Lake Loyera limodzi lokha, lomwe magawo ake ena ndi obvuta kwambiri kuwamvetsetsa, timayesedwa poganiza kuti pali njira inanso yomwe Mulungu angadziwululire kwaife mosiyana ndi m'mene anachitira m'Baibulo. Komanso popeza umunthu wathu wachibadidwe uli wachinyengo ndi wolakwika (Yeremiya 17:9), kumakhala kobvuta kubvomereza zowona zeni zeni za Mau a Mulungu. Ambiri mwa okhulupirira anzathu anatayika chifukwa chofuna kukwaniritsa zofuna zawo, ndikuchita zonse mogwirizana ndi

maganizo awo osati pofunitsitsa kukwaniritsa zofuna ndi cholinga cha Yehova Mulungu chomwe chimapezeka mu Baibulo.

Panopa titawonetsetsa bwino, tingazindikire kuti a khristu ambiri sangathe kufotokoza mokwanira komanso momveka chifukwa cheni cheni chimene iwo amapitira ku tcharitchi. Nthawi zina ngakhale abusa ena samadziwa kweni kweni kufunikira kwa chipembedzo mu choonadi koteru, ndi chifukwa chake timawona kuti ndiwo amayamba kutsogolera utchimo mu mpingo. Pafupi fupi mipingo yonse padziko lapansi lero, palibe mpingo womwe umatsogoza Mulungu mu zochita chita zawo za tsiku ndi tsiku. Ichi ndi chifukwa chimene chinapangitsa kuti ngakhale omasulira Baibulo la Chichewa ndi zilankhulo zina kuno ku Afrika, ataye njira yeni yeni ya kamasuliridwe koyenera, komveka komanso kopereka chithunzi thunzi cheni cheni cha chipulumutso m'cholinga chochokera kwa Mulungu.

Onani zitsanzo zomwe zapatsidwa pansizi:-

CHIPEMBEDZO	NJIRA INA YA ZIKHULUPIRIRO ZOMWE NDI ZOSIYANA NDI NDONDOMEKO YA BAIBULO	PHINDU KWA ANTHU OMWE AMAKHULUPIRIRA CHIPEMBEDZO CHA MTUNDU OTERE
1. MBONI ZA YEHOVA	Amasindikiza mabuku ena pamwamba pa Baibulo omwe amawaonanso ngati Mau owuziridwa ndi Mulungu	Samafuna kuti azibvutika kwambiri pofufuza zowona zeni zeni mu Baibulo moganzira ndi chiphunzitso chimene akuphunzitsidwacho; poyerekezanso ndi chomwe chidalembedwa mu mabuku awo koteru, akawone ngati mamasulidwewo ali chimodzi modzi ndi Buku Lopatulika. Sayenera kupereka yankho lomveka ku funso lililonse lokhudza Buku Loyera ayi. Mabuku osindikizidwawo ndi

		okwanira. Palibe phindu chifukwa chotsatira chake ndi imfa.
2. AROMA (AKATOLIKA)	Amakhulupiranso kuti zonse zonedwa ndi Papa kapena maganizo a ansebe, ndi Mau Oyera a Mulungu	Sizifunikanso kuwerenga Baibulo ayi. Kale a chikatolika san'kalola kuti a khristu awo aziwerenga Baibulo ndipo chidali chinthu choletsedwa mu mpingo wawo. Amakhulupiranso zonena anthu kwambiri osati kuchitapo kanthu kuti anthuwo adzionere okha zolembedwazo mu Baibulo ayi. Palibe phindu popeza chotsatira chake ndi imfa.
3. A MORMONI	Ali ndi Buku lotchedwa "Buku La Mormoni". Baibulo samaliwerenga chifukwa kwa iwo si Buku Lopatulika.	Samawona kufunikira kokhulupirira zolembedwa mu Baibulo zomwe kwa iwo ndi zobvuta kuzitsata komanso kuzimvetsa. Buku la Mormoni limanena kuti chipulumutso chidzafika kwa anthu onse a padziko ngakhale kuti sanamve Mau ndi kukhulupirira. (Ife timadziwa kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu ndipo limatiwuzwa kuti onse omwe sanamve Mau a chipulumutso amafa, mchimbuzi mbuzi (mkusazindikira) momwemonso alibe chiyembekezo ndi chipulumutso chifukwa sadadziwe kanthu. Adzafa chifukwa chosafuna kumvera komanso kulemekeza Mau a Mulungu Namalenga.
4. OKHULUP	Amakhala ndi chikhulupiriro chakuti	Amakhala ndi chikhulupiriro choti zonse zomwe iwo amachita

IRIRA POBADWA NSO MWATSOP ANO NDI KULANDI RA CHIPULU MUTSO MWA AMBUYE WATHU YESU KHRISTU	ali ndi “Kanthu kowala mu mtima mwawo” komwe amati ndi “Mzimu Woyera”	ndiye zokhoza. Amaganizanso kuti Mzimu wa Mulungu umawatsogolera komanso umawauzira komanso kuwathandiza kulosera ngakhale kuti imakhala munjira zomwe nthawi zina sizingagwirizane ndi ndondomeko ya Mulungu yomwe ndi yowululidwa mu Baibulo. Ngati munthu asiyana ndi mfundo ya m’Baibulo kapena kuti samafuna kumvera zolembedwa m’Baibulo omwe ndi Mau a Chiuta, zotsatira zake ndi imfa. Sitiyenera kuwumirira pa zinthu zomwe ife timawuzidwa ayi, koma titsate zolembedwa m’Baibulo popeza tikudziwa kuti ndi Mau ake.
---	---	--

Zonsezi zikhoza kutitsimikizira kuti ndi kofunika kwambiri kubvomereza chipulumutso cha Baibulo kutidi ndiwo Mau a Mulungu; Ndipo kuti ndi koyenera kuwerenga mofufuza, ndi kulaka laka kukhala odziwa zambiri za magawo ake a Buku Lopatulika pa chipulumutso chathu. Mfunso ndi lakuti, tiri ndi Baibulo limodzi lokha, nanga ndi chifukwa chiyani pali mipingo yosiyana siyana yambiri? Mfunso lingayankhidwe bwino pokha pokha ngati tifufuza cholinga cha mipingoyo payokha, momwe mpingo wasankhira pa kachitidwe ka zinthu zina mosiyana ndi m’mene Baibulo limafotokozera za kachitidweko. Mwachitsanzo, Mzimu wa Mulungu; maganizo ake, chipembedzo ndi ulaliki umalalikiwira mosiyana kapena mofanana kwambiri ndi zomwe zinalembedwa mu Baibulo lomwe ndi Buku Lopatulika. Koma chachikulu n’kudziwa kuti pochita zinthu zathu, tiyenera tichite monga Baibulo limatifotokozera osati zosiyana ndi Mau a Chiuta pofuna kukwaniritsa zofuna ndi zolaka laka zathu ayi. Ngati mufuna kupeza mpingo owonadi, chikhulupiriro chimodzi choonadi ndi ubatizo komanso chiyembekezo chimodzinsu mwachilembo chake (Aefeso 4:4-6); tikupemphani mukalimbike kwambiri “posaka saka izi m’Baibulo!”

MPATUKO 4: KODI MZIMU WOYERA NDI MUNTHU/CHINTHU?

Mu phunziro 2.1 ndi 2.2, tawonetsa kuti Mzimu wa Mulungu ndimphamvu zake za Yehova, zomwe zimanyezimiranso maganizo ake kopambana. Popeza ntchito yake ya Chiuta imaonetsa mphamvu zake zomwe ndiye Mzimu Wake, kotero, uthunthu Wake wa Mulungu ukadziwike pakati pathu, anthu ena amaganiza kuti Mzimu wa Mulungu ndi munthu ndipo uli ndi thunthu lomwenso limatchedwa kuti ndi Mulungu palokha. Tikafufuza bwino bwino ndinso kufatsa ndi Baibulo moganizira zomwe taphunzira kalezo, tidzawona kuti Mzimu wa Mulungu, ndimphamvu zake komanso maganizo ake. Ngati izi ndi zomwe Baibulo limatifotokozera, ndiye kuti sizingatheke kuti Mphamvu kapena maganizo chabe akhale mu uthunthu monga momwe aliri munthu. Tiyenera kuona apa kuti maganizo, nzeru, mphamvu, machiritso komanso machitidwe sichinthu china chirichonse chomwe chingaoneke mu uthunthu wake ayi. Chitsanzo cha magetsi ndi chimodzi chomwe chingaperekedwe chifukwa magetsi ali ndi mphamvu yomwe imatulutsa zotsatira zake zopindulitsa kwa anthu ogula magetsiwo. Izi sizitanthawuza kuti mphamvu ya magetsi ili ndi uthunthu wina uliwonse ayi koma kuti mphamvu yakeyo iwonekera kwa anthu basi. Chikondi ndi nzeru, ndi zinanso mwa zikhaliidwe za anthu kotero sichinthu chokhala ndi uthunthu wawo mkati mwa munthu ayi. Mzimu wa Mulungu ndiye mphamvu ya Mulungu kuphatikizapo chikondi Chake ngati chimodzi cha chikhaliidwe Chake kotero, sichinthu china chapadera chomwe chingakhale ndi uthunthu wake wake monga ena amanenera ayi. Mphamvu ya Mulungu iri mu uthunthu wake monga mphamvu ya munthu imakhala mwa munthuyo.

Chodabwitsa pa chikhulupiriro cholakwika ngati chimenechi (chomanena kuti Mzimu uli mu uthunthu wake wake wapadera ndi Mulungu), ndicho chakuti akhristu ambiri, amakhulupirira kwamphamvu mfundo imeneyi chifukwa chofuna kukwaniritsa maganizo awo oti pali milungu itatu mwa m' modziyo. Amati ngakhale milunguyo iripo itatu, yonseyo ndi m' modzi mwa Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Yesu Khristu) ndi Mulungu Mzimu Woyera. Anthu omwewo amanenanso kuti Mulungu saali ndi uthunthu Wake, koma timamvanso pena kuti anthu omwewo amati Mzimu Woyera uli mu uthunthu weni weni; Pali chisokonezo apa ndipo mfundo ziwiri'zi zikutsutsana pazokha ngakhale chiphunzitsa chotere'chi amapereka ndi anthu a chikhulupiriro

chimodzi chomwe sichigwirizana ndi Mau a Mulungu omwewo. Ndipo ena amanenanso kuti Mzimu Woyera ndiye atate ake a Yesu Khristu, ife sitingawatsutse pokha pokha ngati iwo akuzindikiradi chomwe akutanthawuza popeza ife timadziwa kuti Mzimu Woyera ndi ochokera kwa Mulungu ndipo kuti ndimphamvu yake ya Yehova yapadera.

Pali chitsimikizo chokwanira chomwe chimawonetsa kuti chikhulupiriro ndi chiphunzitsa cha milungu itatu mwa m'odzi, sichimachokera m'Baibulo ayi koma ku chikunja ndipo sichingapezeke paliponse m'Baibulo'lo. Chifukwa chaichi, tiona kuti akhristu otere amayamba kukhulupiriranso kuti Mzimu wa Mulungu (Mphamvu ya Mulungu) ili ndi uthunthu wake wapadera, kotero, ndi Mulungu ngakhale saali Mulungu. Wina akafunsitsa kuti amvetse bwino maganizidwe otere, amangoti Mulungu Yehova ndi odabwitsa kotero kuti timayenera kungobvomereza izi posafunsa zambiri. Tionetsetse kuti tiyenera kupeza yankho lililonse lokhudza Yehova Mulungu Wathu mu Baibulo, kuti tikapindule pozindikira zambiri za Iye! Sitiyenera kufufuza zambiri za Yehova kwa munthu ayi popeza munthu ndi operewera pamaso pa Mulungu.

Tizindikiredi kuti mayankho operekedwa ndi munthu, yemwe samafuna kuwerenga mavesi okwanira poyankha zinthu zofunikazi, sangakhale olondola chifukwa akuyankha zomwe iye amaganiza osati mu cholinga cha Mulungu ayi. Mulungu ndi odabwitsa komanso wa Mphamvu ndi wokonzeka kutizindikiritsa ndipo ife tidzadziwa kudabwitsa kwake kumeneku maka maka tikawerenga Mau ake osati momvera zoganza za munthu ayi. Tikapanda kutero ndiye kuti taphwanya ndondomeko ya Chiuta, yomwe imanena mwachimvekere kufunikira kwake kochita chifuniro chake. Chifuniro chimenechi chinawonetsedwa mwa Mwana Wake Yesu Khristu:-

“...Pakuti sindifuna, abale, kuti mukhale osadziwa chinsinsi ichi, kuti mungadziyense anzeru mwa inu nokha,...monga mwa bvumbulutso lachinsinsi chimene chimabisika mwa nthawi zonse zosayamba” (Aroma 16:25).

“....anatzindikiritsa chinsinsi cha chifundo chake....(Aefeso 1:9; 3:3).

Ulaliki wa Paulo unayenera ***“....kuti ndizindikiritse anthu chinsinsicho cha Uthenga Wabwino,”*** (Aefeso 6:19; Akolose 4:3).

“...ndiwo chinsinsicho chinabisika...koma anachiwonetsa (mwa Yesu Khristu) **kwa oyer mtima ake....”** (Akolose 1:26,27-28).

Tiyenera kuzindikira kuti tsopano sichingakhale chodabwitsa kuti anthu akulephera kudziwa ndi kuzindikira bwino komanso kukhala ndi chithunzi thunzi chabwino cha Yehova ngati samawerenga modzipereka Baibulo lomwe ndi dongosolo lake. Yense wa ife ayenera kudziwa chikonzero chake chopezeka mu Mau ake; ndipo azindikirensa kuti dzina la chinsinsi la **“Babelo”**, ndiye ndondomeko, chipembedzo chonama chomwe chikambidwa mu buku la Chibvumbulutso 17:5, kuti ndiyedi chimodzi cha **“chinsinsi”** padziko lapansi chotitengera ife kuchiwonongeko. Chipembedzo chotere nthawi zambiri kwa otsatirawo, amati ndi chipembedzo chowonetsa kudabwitsa kwa **“chinsinsi cha mkazi”** lomwe ndi phiphiritso la tchimo (Chibvumbulutso 17:7).

Munthu oganiza motere, ndi amene amapangitsa kuti anthu azilephera kuzindikira bwino komanso kutsekereza kuti anthu akhale ndi chinyezimiro chowona cha Yehova kotero, m'malo mwake, amalimbikira pa mfundo yosathandiza, yogonera pa mphamvu yomwe siimagwirizana ndi chikonzero cha Chiuta. Tiyeni tigwiritse ntchito maganizo athu mogwirizana ndi m'mene Baibulo limatiphunzitsira kotero, tikadziwe zambiri za chipulumutso chake ndipo tikapulumsidwe.

Ndikhulupirira kuti mukhoza kundibvomereza kuti palibe mlaliki wa Uthenga Wabwino m'modzi wolembe Baibulo yemwe ananenapo zoti **“Ichi ndi chinsinsi chodabwitsa kwambiri, simungathe kumvetsa bwino”**. Zomwe timamva m'malo mwake, ndi kutilimbikitsa kuti ndithu tiyenera kuwerenga Mau akewo ndipo mwaichi, tikadziwe komanso kuyesetsa kuchita monga timawerenga m'Mau ake!

Polalika za Uthenga Wabwino womwe tikuphunzira pano, Paulo **“...ananena nawo poganizira za m'malembo, natanthawuzira, natsimikizira kuti kunayenera Khristu kumva zowawa, ndi kuuka kwa akufa....”** (Machitidwe 17:2,3). Ichi ndi chitsanzo chokwanira komanso chandondomeko yomwe ikuwonetsa cholinga cheni cheni cha Chiuta mu Baibulo; tiwonanso kuti ndondomeko yotere ikuyamba ndi mau oti **“...Paulo monga mwachizolowezi...anawapempha kuti iwo aganizire...”** Timawerenga kuti ichi chinali chizolowezi ndi chikhalidwe chake kuwakumbutsa okhulupirira

kuti azikhala ozindikira nthawi zonse (Machitidwe 18:19). Pogwirizana ndi mfundo yomweyi, pamene anathinitsa ulaliki wake ku Akorinto, Paulo *....anafotokozerera kuti aganizire za izi m'sunagoge masabata onse, nakopa Ayuda ndi Aherene...(koma) pamene anatsutsana* (anamukana?)..."(Machitidwe 18:4-6). Onse omwe anatembenuka mtima nthawi'yo, anakhutitsidwa ndi ulaliki wanzeru ndi watanthauzo wa Paulo omwe unkayima pa chikonzero cha Mulungu m'Baibulo; panalibe zoti "ndalota" kapena kuti "ndaona masomphenya" kapenanso "ndaona Yesu m'chipinda mwanga pamene ndimagona pa bedi langa" ayi, komanso kuti "ndinamva mwachisomo chisangalalo chosaneneka mwaine" ayinso. Komanso kudalibe kuti "ndinaangokumana ndi Ambuye madzulo ena ake," ayi. Zochitika zonse panthawiyo zin'katsamira pa Mau ake basi.

Onaninsu kuti Mau owuziridwa amatifunsa ife tonse okhulupirira ndi osakhulupirira onse kuti ayenera kumvetsa ndi kudziwa ndondomeko yeni yeni ya nzeru; ndi chifukwa chake tawerenga kuti *"...anatsutsana paokha.."* (onani kuti kumasulira kwa Mau mu ndime imeneyi sikuli bwino kweni kweni) (Machitidwe 18:4-6). Moteronso ku Antiokeya, Paulo ndi Barnabasi *"...amene polankhula nawo, anawaumiriza akhale m'chisomo chake cha Ambuye...."* (Machitidwe 13:43). Kenaka anayima pa mudzi wa Ikonio, kumenenso *"...analankhula kotero, kuti khamu lalikulu....anakhulupirira..."* (Machitidwe 14:1).

Ndipo pamene anali kuyesedwa pa m'landu wake m'moyo wake masiku omaliza, m'njira yomweyi ya ndondomeko pa chikonzero cha Baibulo, Paulo anatsimikiziranso za chiyembekezo cheni cheni chirin'kudzacho: *"...anawapempha kuti aganizire za chilungamo, kudziletsa ndi chiweruzo zirin'kudza,"* ngakhale oweruza m'landu anakhudzidwa ndikuti *"anadzidzimuka"* pakumva mau ogwira mtima ngati amenewa (Machitidwe 24:25).

Powona kuti kutembenuka mtima kumafunikira kuganiza bwino pa moyo wathu mogwirizana ndi zomwe tawerenga m'Baibulo kotero, tithe kupereka dongosolo la moyo wathuwo m'chiyembekezo chatu pa Mau a Mulungu:-

"...khalani okonzeka nthawi zonse kuchita chotheka kuyankha mfunso lirilonse lofuna kudziwa chifukwa cha chiyembekezo chomwe muli nacho...." (1 Petro 3:15).

Kulankhula mofatsa za chisomo ndi mtendere womwe munthu waupeza chifukwa chokhulupirira Ambuye Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wake, sikufotokozerana chifukwa cheni cheni cha chiyembekezo chokwanira cha Uthenga Wabwino. Kugonera pa maumboni amene munthu analandirira chipulumutso tsiku lina, kumatsimikizira zakusoweka kwa chidziwitso ndi nzeru zeni zeni za Baibulo kotero, munthu sangathe kuyankha molimba mtima ndi momveka bwino, chifukwa chokhalira ndi **“chiyembekezo chirin’kudzacho”**. Kugawana Mau a Mulungu ndiye chinthu chofunikira koposa koma kugawana umboni wa m’mene wina anapezera chipulumutso padziko lapansi, sichinthu chopindulitsa m’moyo weni weni wa chiyembekezo cha chikhristu ayi; ndi moyo wodzikonda ndipo anthu amataya nthawi kuchita izi m’malo mothandiza kuunikira Mau a Chiyeero kwa anthu kotero, nawonso azindikire mokwanira za Baibulo. Chitsanzo ichi ndi chimene anapereka *Paulo* **“...pakuti tilalikira si zaife tokha, koma Khristu Yesu Ambuye,”** (2 Akorinto: 4:5), ndipo uyu ndi amene anali ndi **“...ubale wapadera zedi ndi Yesu”** kusiyanana ndi wina aliyense.

Chitsanzo cha kutembenuka mtima chomwe takamba m’buku lino ngati ndondomeko yabwino ya chipulumutso, ndi chimene chimapereka ubale weni weni waukulu pakati pathu ndi Mulungu nthawi zonse. Potsimikizira izi, zitsanzo zathu nthawi zambiri zikuchokera m’chikhalidwe cha a khristu anzathu oyambirira omwe **“an’kaganizira”** koposa pofuna funa kulondoloza chikhulupiriro chawo maka maka akapezana ndi mabvuto omwe angabwezeretse chikhulupiriro ndi chipembedzo chawo pambuyo (Machitidwe 6:2). Makalata onse a m’Chipangano Chatsopano anatiwunikira kale za nkhan’yi kudzera mwa anthu omwe an’kawerenga makalatawo napindula, ndipo timaona kuti anazindikira ndinso kubvomereza kumene, zonse zomwe zinalembedwazo kotero, anadziwadi kuti Baibulo ndi Mau a chilongosoko. Mwanjira iyi, tikaganizira za a nsembe akulu akulu, tidziwa kuti pa chilamulo cha Mose, tingathe kudziwanso zambiri zokhudza ntchito ya Khristu (A Hebrei 5:3). Ndipo polankhulapo za chikondi cha Mulungu mwa Khristu, Paulo akutilimbikitsa kuti **“...ndiko kupembedza kwanu koyenera...”** Kotero tikadzipeke kwa Iye m’kumvera (Aroma 12:1). Kudzikhuthula kwa Mulungu pomvera mayitanidwe ake m’choonadi ndi kofunikira chifukwa kumachokera mu cholinga cha Mau eni eni a Yehova Ambuye wathu.

Mongoganizira mau amene’wa, tidzaona tokha kuti pa chinthu chirichonse chomwe chiri ndi cholinga pamoyo wathu wa chikhristu, pamafunikira

kuganiza mofatsa komanso mokwanira kuti tilondoloze chilongosoko cha Baibulo chomwe ndi Mau a Mulungu. Tiri ndi udindo waukulu kuonetsetsa kuti cholinga cha Baibulo chikukwaniritsidwa kudzera mu maulaliki ndi chiphunzitso choyenera pakati pathu kotero, Baibulo likamveke bwino komanso kuti lipitirire kudalirika mu umoyo wa anthu onse. Tikatero, sipangakhaleenso chisokonezo china chirichonse chochokera kwa anthu omwe samamvetsa bwino kapena kuti amafuna kubweretsa chisokonezo mu Uthenga Wabwino wopezeka m'Bukuli.

Tikudziwa kuti onse omwe amakhulupirira kuti Mzimu wa Mulungu siuli mu uthunthu wofanana ndi umunthu, amayesetsa kuwerenga tindime tingapo m'Baibulo pofuna kutsimikizira mfundo imeneyi kuti Mzimu wa Mulungu'wo ndi chinthu chomwe sichingawoneke ndi maso athu. Kawiri kawiri, mavesi amene amawerengedwa'wo, amakhala osayenera komanso osagwirizana ndi m'mene Baibulo limafotokozera; mwachitsanzo, ngati *“za nkhoswe ina”* zomwe timawerenga mu Yohane 14:16 kapena kuti *“Mzimu wabvutika”* zomwe matanthawuzo ake kwa iwo samawamvetsa bwino. Takambanso zambiri za izi mu Phunziro 4.3 kuti mzimu wa munthu ukhoza kugwedezeka (Machitidwe 17:16), ukhoza kubvutika (Genesis 41:8) kapena kusangalatsidwa (Luka 10:21). “Mzimu” wake, mwachitsanzo;- makhaliidwe, maganizo ndi cholinga chake zomwe zinagwira ntchito mwa chifuniro komanso mogwirizana ndi cholinga chakecho, zimakambidwa ngati kuti ndi munthu wapadera ndipo izi sizitanthawuza kuti ndi munthu weni weni ayi. Mzimu wa Mulungu nawonso umakambidwanso mwanjira yomweyi ngati munthu weni weni mu uthunthu wake.

Motero, tizidziwanso kuti nthawi zambiri Baibulo limakamba za mau ena ngati anthu eni eni maka maka maina a zinthu zosawoneka ndi maso, monga nzeru zimakambidwa ngati ndi mzimayi pa Miyambo 9:1. Zonsezi zikutiwonetsa chithunzi thunzi chomwe chimachitika pamene munthu ali ndi nzeru muzochita zake; Sipangakhale nzeru ngati palibe munthu kotero, makambidwe a zinthu ngati amene'wa m'Baibulo amagwiritsidwa ntchito ngati kuti ndi munthu weni weni pamene ndi chikhalidwe cha munthuyo. Tinganene kuti zambiri zokhudza nkhani imeneyi tiwerenga mwatsatane tsatane pa Mpatuko wachisanu.

***MPATUKO 5: MAKAMBIDWE OYEREKEZA
UMUNTHU PONENA ZA CHINTHU;***

Ena akhoza kuwona kobvuta kumvetsa za makambidwe oyerekeza kuti satana angakhale ndi uthunthu monga munthu amawonekera mu Baibulo, monga momwe zimakambidwira ndi mau olowa m'malo mwa maina a munthu ndipo izi zimasokoneza anthu ambiri omwe amaganiza kwambiri mfundoyi, pophatikizapo maganizo a chikunja. Baibulo limakamba za zinthu monga nzeru, tchimo, mpingo, ulemerero ndi maganizo ngati kuti ndi anthu, pogwiritsa ntchito mau olowa m'malo mwa maina a zinthu ngati a anthu; koma timawona kuti akhristu ambiri amalimbikira koposa ndi mau oti mdierekezi kapena satana n'kusiya mau ena onse monga nzeru, maganizo ndi ena otero, omwense amagwiritsidwa ntchito ngati momwe mau a satana amalembedwera.

Tiyeni tiwone zitsanzo ziri m'musinzi:-

NZERU KUKAMBIDWA NGATI MUNTHU

“...wodala ndi wopeza nzeru, ndi woona luntha; Pakuti malonda aposa malonda a siliva, Phindu lake liposa golidi woyengeka. Mtengo wake uposa ngale; Ndipo zonse zikukondweretsa sizilingana naye.” (Miyambo 3:13-15).

“...Nzeru wamanga nyumba yake, wasenza nsanamira (zoyimiritsa) zake zisanu ndi ziwiri” (check translation in English Versions- Miyambo 9:1)

Ndime zimenezi powerenga zigawo zina za m'Baibulo, zikuwonetsa kuti nzeru imakambidwa kawiri kawiri pogwiritsa ntchito mlowamalo wa dzina (pronoun) la munthu wa mkazi; Koma chifukwa chaichi, palibe munthu yemwe ananenapo zoti nzeru ngati wokongola, amangoyenda yenda padziko lapansi ngati momwe ziriri ndi mau oti mdierekezi kapena satana; onse amadziwa kuti iri ndi khalidwe chabe mwa munthu kotero, aliyense ayenera kukhala ndi nzeru nthawi zonse.

MPONDA MATIKI NDI UNJONDA ZIKAMBIDWA NGATI MUNTHU

Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa Ambuye awiri: *“....Pakuti pena adzamuda m’modziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa m’modzi, nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma.”* (Mateyu 6:24). (SEE FROM HERE ITALICS*****)

Chuma pamenepa chakambidwa ngati kuti ndi bwana (munthu). Anthu ambiri amayesetsa kupeza chuma ndipo mwaichi, amakhala ndi maganizo oti iwo ndi opambana anzawo onse kotero, ndi mabwana ndi madona. Yesu pa ndime imeneyi, akunena zakuti ife sitingathe kutumikira Mulungu pamenenso tikudzipanikiza kuyesa yesa kusonkhanitsa chuma nthawi imodzi yomweyo. Tiyenera kusankhapo chinthu chimodzi kuti chinthu tasankhacho, tichichite mofatsa ndi moyenera. Chiphunzitso ichi ndi chosabvuta kuchimvetsa m’mau a chilimbitso ndipo ife tikhoza kutolapo maphunziro akulu pamoyo wathu. Komabe, tidziwa kuti pali anthu ena omwe amakhulupirira mawu otere kuti akuyimira chinthu china, ngakhale kuti palibe m’modzi yemwe angatiwuze zeni zeni kuti chuma ndichinthu kapena chirombo chinanso chopezeka chikuyenda yenda padziko lino lapansi monga marmoni.

TCHIMO LIKAMBIDWA NGATI MUNTHU

“....Yense wakuchita tchimo ali kapolo wa tchimolo...” (Yohane 8:34). *“....tchimo limachita ufumu mu imfa; chomwechonso chisomo chikachite ufumu mwa chilungamo....”* (Aroma 5:21). *“....Kodi simudziwa kuti kwa iye amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ake akumvera iye, mukhalatu akapolo ake a yemweyo mulikumvera iye; kapena a utchimo kulinga kuimfa, kapena a umvero kulinga kuchilungamo?”* (Aroma 6:16).

Monga tawona za chuma, tchimo likukambidwanso mofanana ngati kuti ndi munthu (Bwana ndi akapolo ake). Ngakhale zitatani, pamenepa sitinganene kuti zikutsimikizira maganizo ochepa oti Paulo pano an’kalalikira za chinthu chokhala ndi uthunthu wake ndipo kuti chinthucho chinatchedwa dzina loti “tchimo” ayi. Tchimo ndi khalidwe chabe la munthu kotero, liribe uthunthu wina uliwonse ayi ngakhale likukambidwa ngati kuti ndi munthu wokhala ndi uthunthu wake.

MZIMU NAWO UKAMBIDWANSO NGATI KUTI NDI MUNTHU

“...Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa choonadi, adzatsogolera inu m’choonadi chonse; pakuti sadzalankhula za Iye Mwini...”
(Yohane 16:13)

Yesu pano akufotokoza akuphunzira ake kuti tsiku lina adzalandira mphamvu ya Mzimu Woyera, ndipo izi zinakwaniritsidwa patsiku la Pentekositi, monga timawerenga pa Machitidwe 2:3-4, kuti **“...ndipo anaoneka kwa iwo malirime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera,”** womwe unawonjezera mphamvu zawo kuchita zinthu zodabwitsa potsimikizira kuti an’kapangadi zonsezi ndi ulamuliro wochokera kwa Mulungu. Mzimu Woyera siunali chinthu chokhala ndi uthunthu monga ena amaganizira, ndi mphamvu chabe, koma Yesu anakamba ngati kuti ndi munthu, pogwiritsa ntchito liwu la mlowamalo wa dzina la chimuna.

IMFA IKAMBIDWA NGATI KUTI NDI MUNTHU

“...Taonani, kavalo wotumbuluka; ndipo iye wom’kwera, ndi dzina lake ndiye imfa;” (Chibvumbulutso 6:8).

DZIKO LA ISRAELI LIKAMBIDWA NGATI KUTI NDI MUNTHU

“...Ndidzamangitsanso mudzi wako, ndipo udzamangidwa, iwe namwali wa Israeli; udzakometsedwanso ndi mangako...” (Yeremiya 31:4). **“...Kumva ndamva Efraimu alinkulira kotero, Mwandilanga ine, ndipo ndalangidwa, monga mwana wa ng’ombe wasazolowera gori; munditembenuze ndipo ndidzatembenuka; pakuti inu ndinu Yehova Mulungu wanga...”** (Yeremiya 31:18). Tiwona kuti mau ali mu italikisi’wo ndi olowa m’ malo mwa maina a anthu, apa sakukamba za anthu ayi.

Nkhani yaikulu m’ndime zimenezi ndi yowonetseratu kuti m’neneri’yu sakukamba za namwali weni weni kapena ngati munthu ayi, koma dziko la Israeli, lomwe munkhani’yi, yakambidwa ngati anthu awiri – **“...namwali ndi Efraimu...”**; m’njira yomweyo dziko la Great Britain limatchedwa kuti “Britannia” kapenanso kuti **“John Bull”**. Palibe anthu odziwika ndi maina awiri ngati amenewa ayi komabe, pamene maina’wa alembedwa m’ mabuku

ena ndi m'zithunzi zina zirizonse zowonetsa malo, aliyense amadziwiratu kuti akunena za dziko la Great Britain.

ANTHU OKHULUPIRIRA MWA KHRISTU AKAMBIDWANSO NGATI MUNTHU M'MODZI

“...Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiro cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, kumuyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu” (Aefeso 4:13). *“...Pali thupi limodzi ndi Mzimu umodzi...”* (Aefeso 4:4). *“...Koma inu ndinu thupi la Khristu, ndi ziwalo yense payekha...”* (1 Akorinto 12:27). *“...Khristu ndiye mutu wa Eklesia: ndipo ndiyenso Mpulumutsi wa thupilo...”* (Aefeso 5:23). *“...Iye (Khristu) mutu wa thupi, Eklesiayo;ndikondwera nazo zowawazo chifukwa cha inu, ndipo ndikwaniritsa zoperewera za chisautso cha Khristu m'thupi langa chifukwa cha thupi lake, ndilo Eklesiayo;”* (Akolose 1:18,24). *“...pakuti ndinakupalitsani inu ubwezi mwamuna m'modzi, kuti ndikalangize inu ngati namwali woyera mtima kwa Khristu”* (2 Akorinto 11:2). *“...pakuti wadza ukwati wa mwana wa nkhosa; ndipo mkazi wake ali wokonzeka (wadzikonzera ?)....”* (Chibvumbulutso 19:7).

Ndime zonsezi zikukamba za magulu a anthu omwe anali okhulupirira eni eni a Khristu, nthawi zina zokambidwazo zikukhudza “mpingo” ngakhale kuti tcharitchi iyi, ikusokonezeka ndi matcharitchi a chikale omwe tsopano ambiri anasiya ndondomeko yeni yeni ya chipembedzo choyenera.

Okhulupirira mu choonadi omwe akuyesetsa kusunga ndinso kukhulupirira chiphunzitso cha chiyero chochokera m'Baibulo, ndi amene amatchulidwa “namwali woyera mtima”, kuwonetsa kuti ali ndi umoyo wachiyero womwe iwo ayenera kukhala nawo popeza anamva mwambo komanso analandira malangizo oyenera. Ndipo ngati “thupi”, chomwe ndi chiphiphiritso choyenera, chikuyimira umodzi chifukwa thupi liri ndi ziwalo zambiri zomwe zimagwira ntchito yosiyana siyana monganso Eklesia iri ndi maudindo ambiri osiyana siyananso. Pamene tcharitchi ikambidwa ngati “thupi” palibe wina yemwe angasokonezeke ndi thupi leni leni la munthu, moteronso, mdierekezi kapena satana, sayenera kutisokoneza kapena kusokonezedwa ndi chinthu chirichonse chodziyendera pachokha ndi cholinga chakuti chizichimwitsa anthu pa dziko ayi; zikanakhala kuti omasulira Baibulo anagwira ntchito yotereyi bwino bwino, anthu sakanakhala ndi chithunzi thunzi cholakwika cha

mdierekezi ndi satana ngati chomwe chiripo lero'li chifukwa matcharitchi'wa amanamiza anthuwo, pomasulira molakwika motere. Izi zimachitikanso pamene anthu otere akulalikira Uthenga Wabwino m'matcharitchi awo. Anthu ambiri samafuna kuwerenga okha Baibulo modzipereka kuti amvetse bwino zolembedwazo. Tiwerenganso zambiri za izi mu kabuku kena kotchedwa "Matcharitchi Asokera, (Christendom Gone Astray)" lomwe linalembedwa ndi mbale Robert Roberts.

MPATUKO 6: CHIKHULUPIRIRO CHA CALVINI

Zaka chikwi chimodzi zapitazo, bambo wina dzina lake Calvin analalika m'chiphunzitso chake kuti chipulumutso kapena chiwonongeko cha anthu chimadziwikiratu munthuyo akangobadwa. Ife tikamabadwa, iye anati Mulungu amakonzeratu njira yathu mwina kuchiwonongeko kapena chipulumutso; kotero titha kuchita chinthu chirichonse, choyipa kaya chabwino sipangakhale kusintha kwina kulikonse popeza chikonzero chiripo kale. Amanenanso kuti sitienera kudandaula kotero, kuti chidzachitika ndi chiyani pa moyo wathu. Maganizo ofanana ndi amene'wa ayambanso kumveka m'malo osiyana siyana padziko lapansi:-

- ❑ *Ena amanena kuti sikoyenera kweni kweni kumakhala pamodzi n'kumaphunzitsana Baibulo kapenanso kudziwitsana za chipembedzo choyenera pa chipulumutso chathu. Amanenanso kuti kupulumuka tidzapulumukabe bola tikamachita zabwino basi.*
- ❑ *Kuti kuli chinthu china chokhala ndi uthunthu wake ndipo kuti chimatchedwa mdierekezi kapena kuti satana chomwe chimatiwumiriza kuti tizichimwa; ndipo kuti izi zimabweretsa mabvuto m'miyoyo yathu ngakhale ife sitimafuna kuchimwa ndi mabvutowo. Bodza lokhudza maganizo olakwika ngati amene'wa afotokozedwanso momveka bwino mu Phunziro 6.*
- ❑ *Kuti ndi kosafunikira kufuna funa chithandizo chochokera kwa Mulungu pa moyo wathu watsiku ndi tsiku, mwachitsanzo: kusunga bwino, poyenda ulendo wabwino, chitetezo chabwino. Akuti ndi kosafunikira kupempha Mulungu kuti atithandize mu zinthu ngati zimenezi. Tiyenera kudziwa*

chinthu chimodzi chomwe ndi “Gule ndi iwe mwini.” Chipulumutso chidzakhala cha inu osati cha wina aliyense ayi!

- *Anzathu a Evanjeriko amaphunzitsa kuti ndi kosatheka kukhulupirira Baibulo kapena kulimvetsa kumene ngati munthu sangalandire Mzimu Woyera mwapadera.*

Pali zifukwa zokwanira kwambiri kuti ife tisalole zikhulupiriro zofanana ndi zimenezi:-

- *Sizipereka njira yowona yeni yeni yoti ife tizikhulupirira ndi kumvera Mulungu, ndipo mfundo zimenezi zikusiyaniananatu ndi chiphunzitsa cha Mau a m’Baibulo. Mau a Mulungu amatipatsa malamulo kuti ife tiitsate ndinso kumvera Mulungu’yo kotero, Iye akondwere nafe kapena ayi ngati sitimumvera. Yehova anakonza ndondomeko yotere kuti ife tichite mwakusankha kwathu osati mowumirizidwa ayi. Khristu amatiphunzitsa kuti tingalandire chipulumutso “...**Kwa onse akumvera Iye adzalandira chipulumutso...**” (A Hebri 5:9 - **check translation**).*
- *Kalata ya Paulo kwa A Hebri 11, ikuwonetsa kuti Mulungu amakhala pakati pathu kutipulumutsa mogwirizana ndi chikhulupiriro chathu mwa Iye. Munthu akhoza kutaya nthawi yake kumapemphera kwa Mulungu pamene akudziwa kuti zonse zinakonzedwa kale pa nthawi yomwe iye an’kabadwa. Chipembedzo chingakhaleli chopanda tanthawuzo ngati chipulumutso kapena chiwonongeko kwa ife chinapangidwa kale kapena kuti ndi chodziwikiratu. Palibe tanthawuzo lomveka lirilonse ngati munthu sadzalandira chipulumutso mogwirizana ndi chikhulupiriro chake.*
- *Ubatizo ndi chinthu chimodzi choyambirira kuti munthu alandire chipulumutso (Marko16:16); Yohane 3:3-5). Mfundo yotere ndi imene ikukanidwa ndi onse okhulupirira zomwe bambo Calvin ananena. Ngakhale ziri choncho, chipulumutso chidzabwera kwa ife ngati tikhulupirira ntchito yonse ya Khristu (2 Timoteo 1:10); osati mu zinthu zodzera m’chikonzero cha munthu chomwe chimachitika pa ubwana chomwenso ife sitikuchidziwa ndipo sitinachiwone ayi. Tiyenera kuwonetsa kuti tasankha kukhala pafupi ndi Mulungu’yo*

maka maka poyamba, kubatizidwa mwa Khristu Yesu. Aroma 6:15-17 akukamba za ife kuti timasintha mabwana athu panthawi yomwe tikubatizidwa, kusintha kuchoka mu utchimo ndi kufika mu umoyo womvera Mulungu kuti tilandire moyo wosatha. “...Kwa iye amene mudzipereka eni nokha, kukhala akapolo ake akumumvera Iye...”. Mau amene’wa odzipereka kumumvera Iye, akuwonetseratu kuti munthu’yo akuchita izi, mwakufuna kwake podzisankhira chimene wawona kuti ndiye cholondola kuchichita; osati maganizo olakwika a Calvinini omwe anthu amawumirizidwa kupulumutsidwa kapena kupita ku chiwonongeko. Tiwone kuti ndondomeko yosankha ndiye ya ufulu komanso yogwirizana ndi cholinga cha Mulungu, kudzera m’kumvera Mau a Mulungu omwe ndi Uthenga Wabwino (Aroma 6:17).

- *Pakhoza kukhala chifukwa chosakwanira ngati Mulungu angatipatse Mau ake kotero, ife tiwatsate pamene Iye watipatsa kale mphotho; tiwona kuti Mau akewo angakhale opanda tanthawuzo m’moyo wathu. Sipangakhalenso tanthawuzo leni leni kuti ulaliki ukhalepo ndipo umveke pamene Baibulo limatikumbutsanso kuti munthu angathe kupulumutsidwa polalikira komanso kumvera Mau ake. “..Mau achipulumutso” (Machitidwe 13:26) ayenera kulandiridwa ndi anthu ofuna chipulumutsocho pochita monga tilangizidwa m’Mau akewo.*
- *Tidzaweruzidwa mogwirizana ndi zomwe tinachita (Chibvumbulutso 22:12). Tiwona kuti ndikobvuta kumvetsa mfundo ya bambo Calvinini ngati ife sitichita kanthu mogwirizana ndi Mau a Mulungu kotero chiweruzo chikhalanso chopanda tanthawuzo. Paulo ananaponso kuti Ayuda adadziweruza okha ndipo sangalandire chipulumutso ngati akana Mau a Mulungu (Machitidwe 13:46). An’kadziweruza okha ndipo anadzikana – Mulungu sanawakane ayi. Tikanena kuti Mulungu amayikiratu munthu pamzere wachipulumutso kapena chiwonongeko ndiye kuti sitikutha kumvetsa Mau a Mulungu omwe ndi achilimbitso; kotero kuti, Mulungu akutiwumiriza ife anthu padziko lapansi kuti tizichimwa kapenanso kuti tizikhala oyera mtima. Tikudziwa kuti Mulungu sanakonzze kuti izi zikhale choncho ayi, koma kuti chifukwa cha chikondi chake, ife tichite mwakusankha kwathu, ndipo amatilangiza kuti tiyenera kusankha molongosoka komanso moyenera pomvera Iye chifukwa ndi amene anatilenga. Timadziwanso*

kuti chifukwa chakuti Adamu anachimwa m'munda muja, "...imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa..." (Aroma 5:12). Ichi ndi chifukwa chake anthu amafa, chilango chomwe munthu analandira chifukwa cha tchimo (Aroma 6:23) osati chifukwa chakuti Mulungu anawawumiriza anthu kuti akhale ochimwa kalelo Adamu asanachimwe ayi.

- *1 Akorinto 10* ndi ndime zina m'mabuku a m'Baibulo, ndi zina zomwe ndi za chitsanzo ngati zomwe zimawonetseratu zitsanzo za anzathu akale omwe anali pa ubale wabwino ndi Yehova koma kenaka anachimwa, ndipo izi ndi zitsanzo zokwanira kwaife ngati okhulupirira. Mongoganizira kuti anthu amatha kuchimwa, **"kusoweka chisomo,"** (Agalatiya 5:4) zitanthawuza kuti palibe opulumutsidwa mwa "chibadidwe" ngati momwe gulu la bambo Calvini limanenera. Ife tikhoza kulandira chipulumutso ngati tiyesetsa kusunga ndi kumvera Mau a Mulungu (1 Timoteo 4:16).
- Yesu anaphunzitsa momveka bwino kuti tiyenera kuzindikira Mau a Mulungu osati mowumirizidwa ayi koma modzisankhira tokha titazindikira kufunikira kwake **"...Yense owerenga Mau azindikire...."** (Mateyu 24:15). Mwanjira yomweyi, tidziwe Mau'wo, osati kuvumirizidwa ayi koma mwakusankha kwathu. Izi zikufanananso pamene Yesu ananena kuti **"...Yense yemwe ali ndi makutu, amve ndithu,"** kapena tinene kuti azindikire. Kukhala ndi makutu kuti amve choncho, kumafanananso ndi kuwerenga Mau a Mulungu. Izi ziri motero popeza Mzimu wa Mulungu umadziwikanso koposa m'Mau ake a Mulungu kotero, Yesu anati Mau owuziridwawo **"...ndiwo Mzimu"** ndi moyo (Yohane 6:63); Sizingatheke kuti Mzimu wa Mulungu ugwire ntchito mwa munthu popanda Mau ake kotero, munthu'yo amvere Mau akewo. Mau ndi Mzimu wa Mulungu zimagwira ntchito pamodzi ndipo cholinga chokhala ndi izi ndi kukwaniritsa chinthu chimodzi.
- **"...Ndipo yense yemwe angathe** (angamve kapena angamwe).."
....iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere...." (Chibvumbulutso 22:17), pomvera, kuzindikira, komanso kubvomereza Mau a Moyo opezeka mu Uthenga Wabwino. Apa zingachitike chonchi pokha pokha munthu'yo wachita izi podzisankhira yekha kulandira

chipulumutso osati monga gulu la bambo Calvinini ndi ena onse amanenera ayi. Kotero, Machitidwe 2:21 “..Yense amene adzayitana dzina Lake (la Ambuye) la Khristu, adzapulumutsidwa..” pobatizidwa m’dzina lake la Yesu.

MPATUKO 7: “MUDZALANDIRA MPHATSO YA MZIMU WOYERA” (Machitidwe 2:38).

Petro analankhula kwa chikhamu cha anthu chomwe chinasonkhana pa tsiku la Pentekositi, pomaliza m’ndime ya 38 kuwapempha anthuwo kuti alape, abatizidwe ndinso kulandira mphatso ya Mzimu Woyera. Makambidwe amenewa a mphatso za Mzimu Woyera an’kakhudza kwambiri ophunzira ake a Yesu Khristu; monga mphatso zolankhula m’malirime kwa anthu omwe an’kabwera kumalo otere kuti uthengawo umveke bwino kwa anthu omwense san’kamva zilankhulidwe zina; mwanjira imeneyi malirime’wo anakwaniritsa ulosi wa Yoweri wopereka mphatso ya zozizwitsa (Machitidwe 2:16-20). Choncho, ndizomveka ndithu kuganiza kuti Petro adaalonjeza Mphatso za Mzimu Woyera kwa gulu lija kuphatikizapo a Yuda omwe anamveranso zomwe iye an’kalalikira. Khamu lija panali a Yuda osati a mitundu (a mitundu anali kumverera kuchokera patali ndi khamulo [Machitidwe 2:5]). Ulosi wa Yoweri pa nkhani ya mphatso unakhudza mogwirizana ndi a Yuda omwe anasonkhana pa nthawiyo. Kotero, Petro an’kanena izi kwa a Yuda aja “...*Pakuti lonjezoli liri kwa inu ndi ana anu....*” (Machitidwe 2:39), mwina tinganene kuti moganizira ulosi wa Yoweri, Petro an’kafotokoza kuti mphatso za Mzimu zidzapatsidwa kwa a Yuda ndi ana awo (Machitidwe 2:17-21; cp Yoweri 2:28-32). Chachikulu chomwe chinganenedwe apa ndi chakuti mwina Petro ankatanthawuza kuti Mphatso ya Mzimu Woyera, ya zozizwitsazi, zidayenera kupatsidwa kwa anthu omwe ankamvera’wo ndi ana awo okha komanso; simphatso zonse zomwe zinapatsidwa kwa aliyense wa iwo koma kwa anthu ochepa. Izi ndikukamba choncho moganizira za ulosi omwe ulipo pa nkhani’yi ndi zina zomwe a tumwi anafotokoza pokhudza mutu umene’wu.

Tawona kuti pakutha kwa chirumika choyamba (monga m’mene zinaririri patapita zaka 70 pamene Petro analankhula za mau amene’wa) Mphatso za

Mzimu zinali zitatha. Mbiri'yi ikutsimikiziranso zolembedwa m'mabuku a mbiri yakale yomwe ikuwonetsa kuti izi zinasiya kuwoneka mzaka zomwe zakambidwa pamwambapa. Mphatsozo zinalipo kotero, timawerenga: **“...ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzayitana...”** (Machitidwe 2:39). Onani kuti a mitundu akukambidwa ngati **“onse akutali”** mu Aefeso 2:14-17).

Tizindikiranso kuti zomwe zinachitika pa Machitidwe 2 ndi gawo lochepa lokha lomwe linakwaniritsa ulosi wa Yoweri 2. Kukwaniritsidwa kwathunthu kwa buku la Yoweri 2 kudzachitika pamene mfuko la Israeli lidzathiridwa nk'hondo ndi mayiko ozungulira dziko la Israeli'lo, komanso, pamene mdani wa Israeli'yo adzagonjetsedwe (Yoweri 2:20); komanso pamene Israeli adzalapa machimo ndi kukhala wokondwa m'chipembedzo cha Mulungu chowonadi (Yoweri 2:27). **“...Ndipo kudzachitika m'tsogolo mwake** (mwachitsanzo, zitatha izi), **ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa anthu....”** (Yoweri 2:28). Pokha pokha titawonanso zizindikiro zeni zeni zomwe Yoweri analosera kale monga zimene'zi, ndi pamene tidzakhutitsidwe kuti zikuchitikadi monganso zinachitikira pa Machitidwe 2.

Lonjezo lolandira Mphatso za Mzimu Woyera pamene munthu atangobatizidwa tingathe kuliwerenga m'ndime zingapo lero lino. Pali Mzimu Umodzi, omwe ungasidziwike kwa anthu m'njira zosiyana siyana (1 Akorinto 12:4-7; Aefeso 4:4). M'chirumika choyamba, izi zin'kawoneka mu zozizwitsa; lero mphatso'zi zinachotsedwa ndipo ndi zomveka kuwona kuti “Mphatso za Mzimu Woyera” zinakwaniritsidwa mwanjira zingapo zokha osati njira zonse monga mwa maulosi a aneneri ayi. Kotero, tiri ndi chiyembekezo chokwanira kuti ulosi wa Mphatso zonse zotsala'zo zidzakwaniritsidwabe nthawi'yo ikadzafika monga Mwini anakonzera. Mphatso ya Mzimu Woyera ingatanthawuzidwenso kuti **“Mzimu Woyera”** kapenanso kuti **“Mphatso zomwe Mzimu Woyera zimapereka”** komanso kuti **“zizindikiro zomwe zimawoneka mwa Mzimu Woyera”** mwachitsanzo; Mphatso ya chikhulupiriro, lonjezo la chipulumutso chathu. Pali malo ambiri omwe awonetsa kuti Mau a Mzimu ali ndi **“Umwini”** kunena kuti **“zonse zochitika zimachokera kwa Mwini Wake Mulungu mwakukula m'chizindikiritso** (chathu) **cha Mulungu;** (Akolose 1:10). Ndime imeneyi ikutanthawuza kuti Mulungu alinso ndi nzeru zomwe ife tiyenera tikhale nazo kuti timuzindikire moyenera. **“Chikondi cha Mulungu”** ndi **“Chikondi cha Khristu”** (1 Yohane 4:9; 3:17; 2 Akorinto 5:14) chikuyimira chikondi chimene Mulungu ndi

Yesu Khristu ali nacho paife anthu; kapena chikondi chomwe ife tiri nacho kwa Khristu ndi Mulungu. **“Mau a Mulungu”** angathanthawuze mau okamba za Yehova, kapenanso Mau ochokera kwa Mulungu. Choncho, Mphatso “ya” Mzimu Woyera ingayimire mphatsozo ndi gawo limodzi la Mphamvu za Mzimu Woyera.

MPHATSO ZA MZIMU: CHIKHULUPIRIRO?

Aroma 5:16 ndi 6:23 akukamba za chipulumutso ngati **“Mphatso”** yomwe ingafananizidwe ndi **“mphatso”** ya Mzimu m’Machitidwe 2:38. Ndizowona kuti mau opezeka pa Machitidwe 2:39 akutikumbutsa ulosi wa Yoweri m’ndime 2:32 pokhudza chipulumutso ngakhale kuti iri silingakhale tanthawuzo leni leni la mphatso ya Mzimu. Pamene Petro anakambapo za Mphatso kuti idzakhala ya anthu omwe **“ali kutali”**, anaganizira mau olembedwa pa Yesaya 57:19: **“Mtendere, mtendere** (ndi Mulungu kudzera m’chikhululukiro) **kwa iye amene ali kutali...**” (Aefeso 2:8) akufotokozera za Mphatso kuti ndi chipulumutso ponena kuti **“Mwa Mzimu Umodziwo** (mphatso imeneyi) **ife tonse tiri ndi malowedwe kufika kwa Atate”** (2:18). Izi zikuwonetsa kuti Aefeso 2:13-17 akukamba zonsezi moganiziranso zonedwa pa Yesaya 57:19: **“...Inu amene munali kutali kale, anakusendezani mukhale pafupi m’mwazi wa Khristu. Pakuti Iye ndiye mtendere wathu...**(amene) **anadza, nalalikira Uthenga Wabwino wa mtendere kwa inu akutali...**” (Aefeso 2:13-17). Yesaya 30:1 akudzudzula a Yuda pofuna funa chipulumutso m’njira yosagwirizana ndi chikonzero cha Mulungu koma potsata njira yawo yawo n’kutaya ndondomeko ya Mzimu wa Mulungu: Iwo **“...anapangana pangano opanda Mzimu wanga, kuti awonjezere** (m’ malo mochosera) **utchimo ku utchimo”**. Ndipo Yesaya 44:3 akupitiriza kufotokoza kuti adzakhululukira ana a Israeli mofanana ndi m’mene adzachitire ndi anthu onse okhulupirira: **“...Pakuti ndidzathiramadzi padziko limene liribe madzi, ndi mtsinje pa nthaka yowuma** (yowuma, yopanda chipatso mu uzimu [Yesaya 53:2]) **ndidzathira Mzimu wanga pa mbewu yako, ndi mdalitso wanga pa ana ako”**. Tiwone kuti mdalitso wa mbewu ya Abrahamu, uli m’chikhululukiro cha iwo kudzera mwa Khristu Yesu (Machitidwe 3:25,26) omwe apa ungafanane ndi kuthiridwa kwa Mzimu pa a Yuda aja. Izi kotero, ndi zomveka tikawerenga Yoweri 2 ndi Machitidwe 2 pamodzi. Agalatiya 3:14; akufotokozera nkhani’yi mowonjezerapo ponena, **“...Kuti dalitso la Abrahamu** (chipulumurso cha tchimo) **libwere mwa Yesu Khristu; kotero, lichite kwa a mitundu; kuti tikalandire lonjezo la Mzimu’yo mwa**

chikhulupiriro” Moteronso, 1 Akorinto:6:11 akambanso zoyeretsedwa ku machimo athu, “...*mwa Mzimu wa Mulungu wathu*”. Pali kufanana koposa pakati paife polandira “...*chisomondi utumwi....chiyanjanitso....mwa Mzimu* (Aroma 1:5; 5:11; 8:15), kuwonetseratu kuti poyera kufananiza kapena titi kulumikiza mfundo ya Mphatso (chisomo) ya Mzimu ndi chikhululukulo zomwe zotsatira zake ndi utumwi pakati pa anthu. Zonsezi zikuyendera limodzi m’kulumikizana kotereku. Tawona kuti mwambiri, Chipangano Chatsopano chikufotokozera momveka zonse za m’Chipangano Chakale mogwirizana ndi maganizo ndi kazindikiridwe ka a Yuda. M’mabuku asanu oyambirira ndi buku la Yoswa m’Buku Lopatulika, Mulungu analonjeza kupereka Dziko la Malonjezano kwa anthu ake – “...*Dziko lomwe Ambuye Mulungu wako anakupatsa iwe kuti ulitenge...*” Simau a chilendo, mofanana ndi dziko limeneli, tiwona kuti Mulungu akulonjezanso “*chipulumutso*” m’mau amene’wa a malonjezano otenga dziko; Iyi choncho, ndi mphatso ya Mulungu yomwe tonse tiyenera kuyiyembekezera ngati tachita bwino m’moyo wathu maka maka ngati tikhululukidwa machimo athu.

Agalatiya 3:2,5 cp 3:8-11; Paulo akufotokoza za kufanana kolandira Mzimu ndi kulandira madalitso operekedwa kwa Abrahamu pa chipulumutso ndi chikhululukiro cha tchimo. “*Lonjezo la Mzimu* ” (Agalatiya 3:14) likukambidwa motsatana komanso popitiriza za malonjezano onse operekedwa kwa Abrahamu.

Petro anawafunsa a Yuda kuti alape machimo asanalandire Mphatso; Izi zikutanthawuza kuti aliyense payekha, adayenera kupemphera modzipereka kupempha chikhululukulo kwa Atate. Mwaichi, zikuwonetsa kuti tiyenera kukhulupirira kuti Mphatso ya Mzimu ndi yankho ku pemphero la mphamvu kwa Ambuye. “...*Kupereka zinthu zabwino kwa iwo omwe apempha...*” m’pemphero kufanana ndi kupereka Mzimu Woyera (Mateyu 7:11; cp Luka 11:13). Afilipi 1:19 afananizanso “...*mwa pembedzo lanu, ndi mwa kupatsidwa kwa Mzimu wa Yesu Khristu...*” . Mofanana ndi nkhanu imene’yi 1 Yohane 3:24 akunena kuti tinapatsidwa Mzimu chifukwa cha kumvera malamulo kwathu; Ndime 22 ikunena kuti kumvera malamulowo kumapangitsa mapemphero athu kwa Mulungu kuti amveke komanso kuti ayankhidwe. Chon’cho, chitsimikizo chathu chimagonera pa mayankho a mapemphero athu zomwe zikutsimikizira kuti mapemphero athuwo amamveka ndipo amalandiridwa ndi Mulungu (1 Yohane 5:14) ndi kuti tiri ndi Mzimu

(mphamvu m'Mau ake[1 Yohane 3:21,24; 4:13]), ndipo zonsezi zikutifotokozera chinthu chimodzi chofanana pa chipulumutso chathu.

M'njira imeneyi, ya *"...chisomo (mphatso) ,"* ya *Ambuye Yesu Khristu, tikukhulupirira kuti tidzapulumuka*" (Machitidwe 15:11). Tiwonanso kuti "chisomo" nthawi zambiri chikukhudzidwa ndi pemphero loyankhidwa (mwachitsanzo Eksodo 33:12; 34:9; Numero 32:5; Masalmo 84:11; 2 Akorinto 12:9; A Hebri 4:16 cp. Vs.3). Zekariya 12:10 akunena za matsanulidwe a *"Mzimu wa chisomo ndi wakupembedza"* kwa a Yuda. Izi zikutsimikizadi zomwe takamba kale kuti pemphero limabweretsa mphatso ya Mzimu kudzera m'chikhululuko cha tchimo, ndipo kuti kuperekedwa kwa Mzimu poyankha pemphero kwa munthu, kunawoneka m'chirumika choyamba ndikuti kudzawonetsedwanso m'masiku omaliza pamene Yesu adzabwera. Moteronso, Paulo ananenapo za *"Mphatso ndi mayitanidwe a Mulungu"* kudzera m'kulapa utchimo ndi chikhululukiro (Aroma 11:29).

NKHOSWE (MPUMUZI)

Mofanana ndi m'mene tafotokozera pamwamba'pa za mphatso za Mzimu, malonjezano a Nkhoswe (Mpumuzi) pa Yohane 14 ndi 16 zikufanana m'njira yomwe'yi. Izinsu (malonjezano a Mpumuzi) choyamba zin'kakhudza mphamvu za zozizwitsa zomwe zinaperekedwa kwa ophunzira ake a Yesu, omwensu analandira malonjezano'wa koyambirira kotero, ife tikukhudzidwa osati polandira mphamvu za zozizwitsa ayi koma kudzera m'Mau ake. Mphatso'zo zidayenera *"...adzakuphunzitsani inu nonse, nadzakumbutsa inu ndi kubweretsa zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu"* (Yohane 14:26), izi zinachitika pothandiza kulemba "Uthenga Wabwino". Liwu loti "kukumbutsa" palokha, likuwonetsa kuyikidwa kwa malire a malekezero a malonjezano a zozizwitsa za Nkhoswe (Mpumuzi) yobwerayo pakati pa Ophunzira ake a Yesu, omwe anali ndi Yesu pamene Khristu'yo an'kafalitsa Uthenga Wabwino. Ndipo ndi ophunzira a Yesu okhawa amene angathe kukumbukira Mau a Yesu Khristu'yo omwe anakumbutsidwanso ndi Nkhoswe (Mpumuzi) pa nthawi'yo osati lero ayi. Mau a malonjezano a Nkhoswe akuwonetsedwa komanso kukumbutsidwa m'Mau ake, Buku Lopatulika lomalizidwalo. Mwanjira yotere, tiyenera kutsimikizira kuti malonjezano a Mzimu, anakwaniritsidwa m'zozizwitsa zochitika m'chirumika choyamba ndipo kuti tsopano ife, tikulandira nawo malonjezano'wa kudzera m'ntchito

zotsatira pa zomwe zinachitika kale ndi Mzimu'wo mwa malembo Oyera omwenso ndi Mau a Mulungu omwe amapezeka m'Baibulo.

Mongowerenga zimenezi m'Buku limene'li, tikuwoneratu kuti Mzimu wa Mulungu unawululidwa m'malembo Oyera kalelo, koma kuti kuwululidwa uku sikunali kokwanira pafananiza ndi kumalizidwa kwa (polemba) Baibulo lomwe lero tiri nalo lodzaza ndi Mau ake onse (1 Akorinto 13:9-13). Tikutsimikizidwanso kuti Mphamvu ya Mzimu Woyera itachotsedwa pamene Chipangano Chatsopano chinamalizidwa kulembedwa, palibenso mau ena aliwonse ochokera kwa Mulungu omwe analembedwa m'buku lina lililonse. Ena otsatira zipembedzo zina amanena kuti mabuku a korani, mormoni ndi ena otero, amati analembedwanso mogwirizana ndi mphamvu ya Mulungu pofuna kukonza zolakwika zimene zinalembedwa m'Babibulo. Izi zonse sizowona chifukwa chakuti, Mphamvu ya Mulungu ya Mzimu Oyera ndi yokhayo yomwe inathandiza kuwonetsa chisomo ndi Mphamvu ya Mulungu pakati pathu. Zizindikiro zonse zowonetsa kuti Baibulo ndi Mau eni eni a Mulungu ziripo ndipo zimawonekabe mpaka lero. Mau omwe analosedwa kale'lo amawonekanso ndipo akugwira ntchito modabwitsa powona ndi maso athu zomwe kalelo anzathu sanaganizire kuti zingawoneke, zikuwoneka ndithu mpaka lero. Chon'cho tiyenera kukhulupirira komanso kukhutira kuti Chipangano Chakale ndi Chatsopano zonse, ndi Mau a Mulungu komanso kuti tiyenera kudalira pa Malembo amenewa chifukwa palibenso lembo lina loposa chitsimikizo chimene'chi chopezeka m'mabuku onse a m'Buku Lopatulika lomwe ndi Baibulo.

Motero, munthu aliyense adzakhala okhutira ndi odzazidwa komanso okhala ndi chikhulupiriro cheni cheni, powerenga za kudzazidwa kwa mphamvu ya Mulungu yowululidwa m'Malembo.

MPATUKO 8 : ZIZINDIKIRO IZI ZIDZAWATSATA IWO AKUKHULUPIRIRA (Marko 16: 17)

Anthu ena amanena kuti chifukwa cha mau olembedwa m'ndime iri m'mwamba'yi, aliyense amene amakhulupirira m'choonadi akhoza kulandira Mphatso ya machiritso. Ngakhale ziri chon'cho, kumakhala kobvuta kwa anthu onena izi kuti atsimikizire zonena zawo chifukwa chosakwaniritsa zonse

zokhudza ulosi wotere, “...*adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzayika manja awo pa odwala, ndipo adzachira...*” (Marko 16:18). Tiwona kuti izi sizinthu zoti zingachitike kwa munthu ongonena zotere koma alibe chikhulupirira chokwanira ayi; awa adali malonjezano eni eni omwe anayeneradi kuchitika kwa okhulupirira Iye. Pokha pokha ngati zozizwitsa zotere zingachitike ndi kukwaniritsidwa kwathunthu lero, ndiye kuti zinanenedwa kuti zidzachitika ndi ife m’nthawi yathu; Koma ngati izi sizikuchitika mokwanira monga timawerenga m’Mau ake okha, ndiye kuti lero Mphatso’zi kulibe, zinachotsedwa chifukwa palibe chizindikiro ngati chimene’chi lero lino pakati pathu. Muyenera kukumbukira m’mene Paulo adagwirira njoka yaululu koma sanalumidwe (Machitidwe 28:3-7), zomwe zinatsimikizira kuti ulaliki wake unalidi ochokera kwa Mulungu.

Mwa akhristu onse omwe akhala akunena kuti ali ndi Mphatso ya Mzimu Oyera mzaka 100 zapitazo, palibe chomwe akhristu amene’wa anachitapo zogwirizana ndi zomwe zinawoneka m’ndime zimene takhala tikuwerenga pamwambazi. Nthawi zonze akamachita zozizwitsa zawo sizigwirizana ndi momwe zinali kuchitikira kale panthawi ya Yesu kapenaso akuphunzira ake a Yesu, zomwe zimatsimikiza Malembo Oyera kuti Mphatso’zi zinachotsedwadi. Chotero, tatsimikiza pano kuti Mphatso ya zozizwitsa in’kalandiridwa kale ndi ena mwa okhulupirira m’chirumika choyamba, koma inachotsedwa pamene Chipangano Chatsopano chinamalizidwa kulembedwa.

Ndime yomaliza mu Marko 16 ikutipatsa ganizo loti zozizwitsa “zotsatira” kwa iwo okhulupirira zinaperekedwa ndi cholinga chapadera kufuna kukwaniritsa ntchito zosanthulidwa mwapadera mu Uthenga Wabwino: “...*zizindikiro izi zidzawatsata iwo akukhulupiriraiwowa anatuluka, nalalikiraponseponse, ndipo Ambuye anachita nawo pamodzi, natsimikizira Mau ndi zizindikiro za kutsatapo...*” (Marko 16:17, 20). Izi zonse zin’kachitika motere chifukwa kudalibe Chipangano Chatsopano koma chitalembedwa, sipanafunikirenso kukhala ndi Mphatso zozizwitsa kwa iwo okhulupirira.

Powona kuti akhristu ambiri akumanena kuti analandira Mphatso za Mzimu Oyera’zi, m’chaka cha 1989 kunakonzedwa Mtsutso pakati pa ine ndi m’bale John Allfree ndipo mbali inayo kunali Pastor John Liliekas. Mutu wa nkhani unali “*Kodi Mphatso zozizwitsa za Mzimu Woyera zikadalipo?*” Tinayitanitsa a khristu ambiri otsatira ma tcharitchi osiyana siyana m’dziko lonse la United

Kingdom, omwe anabwera anapitirira 1,000 kudzamvera m'tsutso'wo. Anthu ambiri adafunsa mafunso awo ambiri ku mbali zonse ziwiri ndipo anakhutitsidwa ndi zonse zomwe zinakambidwa monga tafotokoza pamwambapa. Pali kabuku kakang'ono kofotokoza zomwe zinanenedwa patsiku'li, ndipo mukhoza kuyitanitsa ku adiresi iri komalizira kwa buku lino m'Chingerezi. Ngati mungathe, chonde, itanitsani buku'li m'Chingerezi.

PHUNZIRO 2: MAFUNSO

1. Ndi ati mwa mau apatsidwa'wa omwe akutanthawuzira liwu loti "*Mzimu*"?
 - (a) Mphamvu
 - (b) Kupatulidwa mwapadera
 - (c) Mpweya
 - (d) Mfumbi
2. Mzimu Woyera n'chiyani?
 - (a) Ndi munthu
 - (b) Mphamvu
 - (c) Mphamvu ya Mulungu
 - (d) M'modzi mwa milungu itatu'yo
3. Kodi Baibulo linalembedwa bwanji?
 - (a) anthu analemba maganizo awo
 - (b) anthu analemba zimene anaganiza kuti Mulungu akutanthawuzira mwa iwo
 - (c) Mowuziridwa ndi mpweya wa Mphamvu ya Mzimu wa Mulungu
 - (d) Mau ena anawuziridwa, pamene mau ena sanawuziridwe
4. Ndi zifukwa ziti mwa zotsatira'zi zomwe zikutipatsa cholinga cheni cheni cha Mphatso zozizwitsa za Mzimu?
 - (a) Kutsimikizira zolalikidwa za Uthenga Wabwino
 - (b) Kutukula Eklesia woyambirira
 - (c) Kuwunikira anthu kuti akhale oyeretsedwa
 - (d) Kupulumutsa ophunzira a Yesu ku mabvuto omwe anali nawo.
5. Tingaphunzire choonadi cha Mulungu kuti?
 - (a) Kuchokera m'Baibulo, komanso m'maganizo athu athu
 - (b) Kuchokera kwa Mzimu Woyera potiwuza zoyenera kuchita, pamwamba pophatikizapo kuwerenga Baibulo
 - (c) Kuchokera m'Baibulo lokha basi
 - (d) Kuphunzitsidwa ndi atsogoleri a mpingo, ansembe ndi a Pasitala
6. Tchulani zina mwa Mphatso za Mzimu zomwe zin'kaperekedwa m'chirumika choyamba.
7. Kodi Mphatso za Mzimu zinachotsedwa liti? Zimatheka lero kulandira Mphatso za Mzimu?
8. Nanga Mzimu Woyera umagwira bwanji ntchito m'miyoyo yathu lero?

Mukayankha chonde tumizani mayankho anu ku imodzi mwa ma adiresi alembedwa komaliza kwa buku lino:

PHUNZIRO 3

**MALONJEZANO A
MULUNGU**

3.1 MALONJEZANO A MULUNGU OYAMBA

Tafika pozindikira tsopano kuti Mulungu ndindani, nanga amagwira bwanji ntchito yake. Tikatero, ndiye kuti tachotsa zipysinjo zingapo zomwe zimalepheretsa chizindikiritso choyenera pa nkhani zimenezi. Nthawi ino, tifuna tiwonere limodzi zomwe Mulunguyo “....*adalonjezera iwo akumkonda Iye*” (Yakobo 1:12; 2:5) posunga komanso kumvera malamulo (Yohane 14:15).

Malonjezano a Mulungu m’Chipangano Chakale ndiye mzati weni weni wa chiyembekezo cha a khristu. Pamene Paulo an’kayimbidwa mlandu, anafotokoza motsimikiza za mphotho yomwe iye sanali okonzeka kuyitaya ayi, koma m’ malo mwake anakonzeka kutaya zinthu zina zonse ndi cholinga cholandira mphotho’yo: “....*Ndipo tsopano ndiyimirira pano ndiweruzidwe pa chiyembekezo cha lonjezano limene Mulungu analichita kwa makolo athu;chifukwa cha chiyembekezo ichi....andinenera ..*” (Machitidwe 26:6, 7). Iye anakhala nthawi yayikulu ya moyo wake wonse kulalikira “....*Uthenga Wabwino* (nkhani yosangalatsa), *wa lonjezano lochitidwa kwa makolo; kuti Mulungu analikwaniritsa ili kwa ana awo pa kuukitsa Yesu....*” (Machitidwe 13:32, 33). Paulo akupitiriza pa mfundoyi kuti chikhulupiriro mwamalonjezano a Mulungu amene’wa, anatipatsa chiyembekezo chathu cha kuukanso kwa akufa kwaife (Machitidwe 26:6-8 cp. 23:8), anatipatsanso nzeru yakutizindikiritisa za kubweranso kwa Yesu Khristu kudzaweruza anthu komanso kudzakhazikitsa ufumu wa Mulungu (Machitidwe 24:25; 28: 20, 31).

Tikafika apa ndiye kuti maganizo onse a anthu ena omwe amanena kuti Chipangano Chakale ndi mbiri chabe ya kale yokambidwa ndi akulu akulu a ku Israeli tsopano athera pamenepa; chifukwa tawona kufunikira kwake kwa Chipangano (malonjezano) chimenechi pa chipulumutso chathu. Mulungu sanangoganiza chabe mzaka za 2,000 zapitazo kuti basi, lero ndiwapatsa moyo wosatha anthu anga kudzera mwa Yesu ayi. Panali chikonzero chimene’chi kuchokera pa chiyanbi pamene an’kalenga dziko’li:-

“....m’chiyembekezo cha moyo wosatha, umene Mulungu wosanamayo, analonjeza zisanayambe nthawi zosayamba; koma pa

nyengo ya Iye yekha anawonetsa mau ake (okhudza izi) *mu ulalikiro,...*” (Tito 1:2,3).

“...moyo wosathawo, umene unali ndi Atate, ndipo unawonekera kwaife...” (1 Yohane 1:2).

Poona kuti kuchokera pachiyambi, chinali cholinga cha Mulungu kupereka moyo wosatha kwa anthu ake, ndi chodziwikiratu kuti Iye sakanangokhala chete osachitapo kanthu, zaka 4,000 zapitazo zomwe Mulungu’yo wakhala akulumikizana ndi anthu m’nthawi ya Chipangano Chakale. Timawerenga kuti Chipangano Chakale ndi chodzaza ndi maulosi ndinso mauneneri, kuphatikizapo malonjezano omwe akutipatsa ife ndondomeko yokwanira ya chiyembekezo chomwe Mulungu anatikonzera ife anthu ake. Chifukwa chaichi, n’koyenera kumvetsa ndi kuzindikira mokwanira za malonjezano omwe Mulungu Yehova anapangana ndi akulu akulu a chi Yuda omwe ndi ofunikira pa chipulumutso chathu: Kotero, Paulo akutikumbutsa kudzera mwa anzathu a kwa Aefeso kuti asanadziwe izi anali *“...opanda Khristu, munali alendo a padera ndi mbumba ya Israeli, ndinso alendo opanda kanthu ndi mapangano a malonjezano, opanda chiyembekezo, ndi opanda Mulungu m’dziko lapansi....”* (Aefeso 2:12) ngakhale kuti mosakayikira, an’kaganizabe kuti mzochita zawo zakalezo ngakhale zidali za chipembedzo koma m’chikunja momwemo, anali nazo nzeru zowalepheretsa kumudziwa Mulungu. Anali okhutitsidwa kuti ali nacho chiyembekezo mwa Yehova pamene zinthu sizinali choncho. Zonse’zi ndi chifukwa chakuti iwo sanamvetse kweni kweni za malonjezano a m’ Chipangano Chakale aja omwe Mulungu anapanga ndi makolo awo, ndipo ponena zoonza zeni zeni - *“....analibe chiyembekezo, opanda Mulungu m’dziko lapansi...”* Kumbukirani momwe Paulo anafotokozera za chiyembekezo cha a khristu kuti ndi *“....chiyembekezo cha lonjezano limene Mulungu analichita kwa makolo athu...”* ([makolo a chi Yuda] Machitidwe 26:6).

Zimamvetsa chisoni kuwona kuti ngakhale mfundo imeneyi ya malonjezano imawonekeratu kuti ndiyofunikira kuyitsindika pa chipulumutso cha chi khristu; matcharitchi ambiri masiku ano, samawona kufunikira kwake kozindikira izi kotero, a khristu’wa samadziwa malo ambiri okamba malonjezano ofunika’wa m’Chipangano Chakale. Masiku ano, chikhristu, n’kudziwa za m’Chipangano Chatsopano chokha komanso amawerenga ndime zochepa zedi m’Chipangano Chatsopano’cho. Yesu akutsindika kwambiri pa mfundo yotere pofuna kukonza maganizo olakwika ngati amene’wa:-

“...ngati samamvera Mose (mwachitsanzo, mabuku asanu oyambirira a Baibulo omwe Mose analemba) **ndi aneneri, sadzakopeka mtima ngakhale wina akauka kwa akufa...**” (Luka 16:31).

M’maganizo athu a chibadidwe, tingamayese kuti pongokhulupirira za kuukanso kwa Yesu kwa akufa, ndiye kuti takwanitsa zofunika zonse pa chipulumutso chathu (cp. Luka 16:30), koma Yesu anati popanda kuzindikira kokwanira zolembedwa m’Chipangano Chakale, chikhulupiriro chotere sichingakhale chotiyenereza pa chipulumutso chathu pamaso pa Mulungu ndi Ambuye wathu Yesu Khristu.

Akuphunzira ake a Yesu, anabwerera m’mbuyo pa chikhulupiriro chawo Yesu atangopachikidwa kumene ndipo Yesu anazindikira, nawachenjeza kuti ngati sangawonetse chidwi chawo ndi zolembedwa m’Chipangano Chakale, sangaphulepo kanthu.

“...Iye anati kwa iwo, Opusa inu, ndi ozengereza mtima kusakhulupirira zonse adazilankhula aneneri! Kodi sanayenera Khristu kumva zowawa izi, ndikulowa ndi mu ulemerero wake? Ndipo anayamba kwa Mose, ndi kwa aneneri onse, nawatanthawuzira iwo m’malembo onse a zinthu za Iye yekha” (Luka 24:25-27).

Onani momwe Yesu akutsimikizira za momwe Chipangano Chakale chonse chidafotokozera za Iye kalelo. Sindiye kuti akuphunzira ake aja onse anali asanawerengepo zimene’zi, kapena kuti sadamvepo Mau a m’Chipangano Chakale ayi, koma kuti sanamvetse bwino ndi kuzindikira moyenera, koteru, sanathe kukhulupirira mokwanira za Mau’wa. Tiwona kuti kuzindikira kwathunthu Mau a Mulungu, m’ malo momangowerengapo, ndikofunikira kuti chikhulupiriro chathu chikhwime m’choonadi. A Yuda aja an’kanthunthumira mosayenera powerenga Chipngano Chakale (Machitidwe 15:21), koma popeza sanamvetse kuti izi zinafotokozera za Yesu ndi Uthenga Wake Wabwino, sanathenso kukhulupirira zonse’zi choncho, Yesu anawawuza kuti:-

“...Pakuti mukadakhulupirira Mose, mukadakhulupirira ine; pakuti iyeyu analemba za ine. Koma ngati simukhulupirira

malembo a iyeyu, mudzakhulupirira bwanji mau anga? (Yohane 5:46,47).

Tawonani abale, ngakhale a Yuda aja an'kawerenga Baibulo, sanathe kudziwonera Uthenga weni weni wa Yesu, ngakhale m'maganizo mwawo anali okhutitsidwa kuti adzalandira chipulumutso! Yesu anawauza kuti:-

“...popeza analandira mau ndikufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m'malembo (kusanthula moyenera-cp Machitidwe 17:11); musanthula m'malembo popeza muyesa kuti momwemo muli nawo moyo wosatha, ndipo akundichitira Ine umboni ndi iwo omwewo; ” (Yohane 5:39).

Mwanjira yomweyi, anthu ambiri sangathe kuwona Uthenga Wabwino wotere kuchokera m'Chipangano Chakale mpaka Chipangano Chatsopano. Samadziwa zambiri za Baibulo m'ndondomeko yofanana ndi imeneyi ndipo iwo, amangowerengapo osazindikira kulumikizana kweni kweni m'mau a zipangano zimenezi kotero, sangathe kumudziwa Yesu m'chowonadi cha Baibulo. Samadziwanso ndondomeko yokwanira ya Mulungu yokhudza Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. N'cholinga cha maphunziro ano kuchotsa kusazindikira ndi umbuli wa mtundu ngati umene'wu, powonetsa mitu yayikulu yikulu ya malonjezano opezeka m'Chipangano Chakale:-

Malonjezano awa ndi a

-m'munda wa Edeni

-Kwa Nowa

-Kwa Abrahamu

-Kwa Davide

Malonjezano amenewa tingawerenge m'mabuku asanu oyambirira (Genesis-Deuteronomo) omwe analembedwa ndi Mose, ndipo ali mu Chipangano Chakale pamodzi ndi aneneri. Zonse zokhudza Uthenga Wabwino zikupezeka m'mabuku amene'wa. Paulo anafotokoza kuti ulaliki wake pa Uthenga Wabwino umene'wu, ndi ***“...osanena kanthu kena koma zimene aneneri ndi Mose ananena zidzafika; kuti Khristu akanve zowawa, kuti Iye, woyamba mwa kuuka kwa akufa, adzalandira kuunika kwa anthu ndi kwa a***

mitundu....” (Machitidwe 26:22,23); ndipo m’masiku ake omaliza, Paulo anakambanso zomwezi:- *“...amenewo anawafotokozera, ndi kuchitira umboni Ufumu wa Mulungu, ndi kuwakopa za Yesu, zochokera m’chilamulo cha Mose ndi mwa aneneri, kuyambira m’ mawa mawa kufikira madzulo...”* (Machitidwe 28:23).

Chiyembekezo cha Paulo, m’khristu wamkulu, chiyenera kukhala chiyembekezo chotilimbitsa ife; Poona kuti komalizira kwa moyo wake kunali kuwala, ifenso tikalimbikira, tidzakhala ndi tsogolo lowala pa chipulumutso chathu. M’mpamvu imeneyi, tilimbikitsidwa kuwerenga mozama ndi mofufuza Mau ake.

3.2 MALONJEZANO A M’MUNDA WA EDENI

Nkhani yomvetsa chisoni kwambiri ya chiyambi cha tchimo pamene munthu anagonjetsedwa ndi tchimo ikugwirizana ndi zopezeka m’buku la Genesis 3. Njoka inatembereredwa chifukwa inanamiza komanso kuyesa Hava; koteru Hava sanamvere Mau a Mulungu. Mwamuna ndi mkazi anapatsidwa chilango popeza iwo onse sanamvere. Kuchoka mu mdima umenewu, kunafika muuni wa chiyembekezo pamene Mulungu ananena kwa njoka’yo:-

“...ndipo ndidzayika udani (mkwiwirano, mtsutso) pakati pa iwe ndi mkaziyo ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yake; ndipo (mbeu yake ya mkazi) idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chidendene chake...” (Genesis 3:15).

Ndime imene’yi, ikukamba zinthu zambiri mwachindunji ndi mwachidule; tiyenera tifufuze kokwanira zinthu zimenezi chomwe ndime’yi ikutanthawuza. “Mbeu” apa ikutanthawuza “mwana wa mkazi” uja komanso ikutanthawuzanso anthu omwe akukhudzidwa ndi “mbeu’yo”. Tiwona komalizirako kuti “mbeu” ya Abrahamu anali Yesu (Agalatiya 3:16), koma ngati ife tikhala “mwa” Yesu, mu ubatizo, ndiye kuti ndifenso “mbeu” (Agalatiya 3:27-29). Liwu ili loti “mbeu” lingagwirizananenso ndi mafesedwe a mtundu wa anthu kapena chinthu; monga tidziwa kuti mbeu yeni yeni imafanana ndipo kuti siimasiyana ndi mbeu yobzalidwa moyambirira

imayenera kuwoneka ngati momwe munthu amawonekera mkalilole (1 Petro 1:23); kotero, mbeu yeniyeni ndi chinyezimiro cha makhalidwe a tate wake.

Momwemonso, mbeu ya njoka ija iyenera kufanana komanso kunyezimira chikhalidwe cha njoka ya m'munda wa Edeni uja monga:-

-kumasulira molakwika dala Mau a Mulungu

-Kunamiza

-Kuwakokera ena ku tchimo

Tiwerenga mu Phunziro 6 kuti palibe munthu kapena chinthu china chirichonse chomwe ena amanena kuti chimalowa mwaife n'kumatichimwitsa ayi, koma kuti mwaife muli:-

-“tiri ndi utchimo” m'thupi lathu la chibadidwe (Aroma 6;6)

-ndife *“munthu wachilengedwe”* (1 Akorinto 2:14)

-munthu wakale, wobvunda m'chikhalidwe chonyansa monga mwa chilakolako chathu” (Aefeso 4:22)

-“munthu wakale pamodzi ndi ntchito zake” (Akolose 3:9)

“Munthu” ameneyu wa uchimo mwaife ndiifeyo tikamangoganiza za tchimo nthawi zonse ndipo Baibulo limati ndi **“m'dierekezi”** yemwense ndi mbeu ya njoka ija. Kotero, ife ndife mbeu ya njoka ija pachibadidwe ngati zochitika ndi maganizo athu nthawi zonse ndi a utchimo.

Mbeu ya mkazi ija idayenera kukhala munthu weni weni wodziwika bwino ndi anthu onse – *“...ndipo* (mbeu ya njoka) *ive udzalalira chidendene chake...”* (Genesis 3:15). Munthu uyu adayenera kuphwanya (kupha) komaliziratu mbeu ya njoka, mwachitsanzo, tchimo – *“...idzalalira mutu wako...”*. Kuphwanya mutu wa njoka n'kupheratu njoka popeza kuti ubongo wake uli m'mutumo, pamene kuphwanya chidendene cha munthu, munthu'yo sangafe amangobvulala chabe. Munthu yekhayo amene angakhale woyenera kutchedwa *“mbeu ya mkazi”* yothetseratu tchimo (njoka) ndi Ambuye Yesu:-

“...*Yesu Khristu amenedi* (pamtanda) *anagonjetsa imfa* (ndipo choncho, mphamvu ya utchimo [Aroma 6:23]), *naonetseratu poyera moyo ndi chosabvunda mwa Uthenga Wabwino....*” (2 Timoteo 1:10-translation?).

“...*Mulungu anatumiza Mwana wake wa Iye Yekha m’chifanizo cha thupi la uchimo ndi chifukwa cha uchimo natsutsa* (nadzudzula) *uchimo m’thupi...*” mwachitsanzo, mdierekezi wa m’Baibulo, mbeu ya njoka (Aroma 8:3).

Jesus “...*anawonekera* (mu uthunthu wa umunthu) *kudzachotsa machimo...*”(1 Yohane 3:5).

“...*ndipo udzamutcha dzina lake Yesu* (kutanthawuza kuti Mpulumutsi); *pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo....*” (Mateyu 1:21).

Yesu ndi “...*wobadwa ndi mkazi....*,” (Agalatiya 4:4) ngati mwana wa Maria, ngakhale kuti bambo wake weni weni anali Mulungu. Munjira yomweyinsu, anali mbeu ya mkazi, ngakhalenso kuti anapatsidwa ndi Mulungu kwa munthu mosiyana kwambiri ndi munthu wina aliyense. Mbeu imeneyi ya mkazi inabvulazidwa mwapang’ono pa chidendene, kotero, bala likhoza kupola, kusiyana ndi kubvulazidwa kophwanyidwa m’mutu monga njoka ija, komwe kukuyimira imfa. Mbeu ya mkazi (Yesu) inalalidwa ndi tchimo, pamene mbeu ya njoka “...*udzalira chidendene chake....*” (Genesis 3:15). Kuluma kwa njoka pa chidendene kumabweretsa chilonda pa kanthawi kochepe, chilonda chomwe chikhoza kupola mosabvutikira kusiyana ndi kuthudzula mutu wa chinthu. M’Baibulo muli ziphiphiritso zambiri monga “*kuthudzula mutu*” (mwachitsanzo, kuphwanya mutu kukhoza kumaliza umoyo wa chinthu [kapena tinene kuti kupheratu chinthucho) zikhoza kutanthawuzanso ulosi uwu wa Yesu kuti anayimena njokayo pa mutu, kapenanso kuti anayipha.

Pogonjetsa tchimo lomwe ndi mbeu ya njoka, Khristu anachita izi choyambirira pa mtanda paja pamene anapachikidwa mwachitonzo, koma anawukanso kwa akufa; onani momwe mavesi tawerenga pamwamaba’wa akunenera za kupambana ndi chigonjetso cha tchimo kalelo. Chilonda cha chidendene chomwe njoka inalalira Yesu, chikutanthawuza za imfa yake yomwe Iye anasauka nayo kwa masiku atatu okha kenaka chilondacho

chinapola. Kuwukitsidwa kwake kwa akufa kukuwonetsa kuti Iye sakanakhalitsa m'manda chifukwa munali mongoyembekezera kuti zilonda zake zipole poyerekeza ndi kuthetsedwa kwaimfa komwe Iye anathana ndi imfayo pa mtanda paja. N'zochititsa chidwi pamene timawerenga mbiri yakale, kuti kunalinso anthu ena amene ankapachikidwa pa mtanda pokhoma zidendene zawo pa mtengo ndi misomali, zomwensho zikufanana ndi zochitika pa nthawi ya kupachikidwa kwa Khristu. Choncho, n'chifukwa chake “...*Yesu anabvulazidwa pa chidendene...*” Mwa imfa yake. Yesaya 53:4,5 akutifotokozera za a Khristu kuti “...*anabvulazidwa...*” ndi Mulungu mwa imfa yake ya pamtanda. Izi zikunena za ulosi umenewu wa pa Genesis 3:15 kuti Khristu anayenera kubvulazidwa ndi mbeu ya njokayo. Ndipo pamenepa, Mulungu anagwiritsa ntchito uchimo womwe Yesu Khristu anakumana nawo kotero, Yesaya akunena za izi kuti Mulungu anabvulaza Khristu (Yesaya 53:10), powunika zoyipa zomwe zinabvulazadi Khristu Mwana wake. Mulungu amachita zinthu zonse pogwiritsanso ntchito zoyipa zonse zomwe zakhala zikuchitika kwa anthu ake kapena pogwiritsa ntchito anthu ochita zoyipa monga mfumu Nebukadinezara.

CHIPINGANO CHA (MKANGANO WA) LERO

Mukhoza kukhala ndi mfunso m'mitima mwanu: “...*Ngati Yesu anathetsa tchimo ndi imfa* (mbeu ya njoka), *chifukwa chiyani imfayo ndi tchimo zikadalipo?*” yankho lake ndiye kuti pa mtanda paja Yesu anathetsa mphamvu ya utchimo mwa Iye yekha: Ulosi wa pa Genesis 3:15 kotero, koyambirira ndi kusiyana pakati pa Yesu ndi tchimo. Tsopano izi zikutanthawuza kuti popeza Iye anatiyitana kukagawana naye m'kupambana kwake, kotero, ifenso tikagonjetse tchimo ndi imfa. Iwo amene sanayitanidwepo kuti akagawane nawo kupambanaku, kapena omwe anakana mayitanidwewo, adzakhalabe mu tchimo ndi imfa. Ngakhale kuti tchimo ndi imfa zimafikiranso kwa onse okhulupirira choonadi, omwensho akhoza kutchulidwa nawo “mbeu ya mkazi” mu ubatizo mwa Khristu Yesu (Agalatiya 3:27-29), angathenso kulandira chikhululukiro cha machimo awo choncho, angathe kupulumutsidwa ku imfa, yomwe ndi chotsatira chake cha utchimo. Mwaichi, Yesu “*anathetsa imfa*” pamtanda (2 Timoteo 1:10), ngakhale kuti cholinga cha Mulungu ndi dziko lapansi sichinakwaniritsidwe kotero, anthu sadzafanso – pomwe imfa siidzawonekanso panso pano: “...*Pakuti ayenera kuchita ufumu* (kulamulira m'chigawo choyamba mu Ufumu wa Mulungu) *kufikira atayika adani onse*”

pansi pa mapazi ake. Mdani wotsiriza amene adzathedwa ndiye imfa” (1 Akorinto 15:25,26).

Tikabatizidwa *“mwa Khristu Yesu”* ndiye kuti timalandira nawo malonjezano okhudza Yesu monga tikuwerenga pa Genesis 3:15; ndipo izi sizimangokhala nkhabakamwa chabe m’Baibulo ayi, ndi maulosi ndi uneneri wa malonjezano eni eni omwe Mulungu anawanenanso kwaife! Monga mbeu ya mkazi, ifenso, tidzapambana pa nkondo ya pakati pa ife ndi tchimo (mbeu ya njoka) panthawi yobatizidwayo. Pokha pokhanso Khristu atabwera ife tisanafe, tidzabvulazidwa moyembekezera pa chidendene monga Khristu anabvulazidwa pamtanda, naafa pa kanthawi kochepe, ifenso tidzafa ngati Yesu akhalabe asanafike kuchoka kumwamba. Koma ngati ndifedi mbeu yeni yeni ya mkazi ya m’Baibulo, ndiye kuti chilonda chimenechi chongoyembekezerachi, chidzapola ndikuti sichidzakhali. Onse omwe amatizidwa moyenera mu ubatizo weni weni wokhawo, womiza m’madzi, amalumikizidwa ndi imfa yake ndi kuukanso kwa Khristu m’chiphiphiritso chotuluka kuchoka kapena titi kubvuuka m’madzi (Aroma 6:3-5).

Ngati ndifedi mbeu yeni yeni ya mkazi, ndiye kuti miyoyo yathu idzanyezimira Mau Ake opezeka pa Genesis 3:15; – payenera kuti pazikhala nkondo yopitirira, yosalekeza mkati mwathu pakati pochita zabwino ndi zoyipa. Mtumwi Wamkulu Paulo, akufotokozerazambiri zokhudza nkondo yaikulu yomwe inkachitika mu mtima mwake (**Aroma 7:14-25**).

Munthu atangobatizidwa mwa Khristu, nkondo imeneyi yomwe ndi tchimo, imakhala mwaife m’chibadidwe chathu, imakulira kulira koteri izi, zimapitirira mpaka moyo wathu wonse (moyo wa Paulo ndi chitsanzo chachikulu mpaka imfa yake). Tidzaona tokha kuti izi zimakhala zobvuta kwambiri kuzipirira chifukwa mphamvu ya utchimo ndi yolimba koteronso imabvuta kuyiphwanya ngati sitingasamale. Koma tikafatsa ndi Baibulo, tidzazindikira ndipo tidzawonanso kuti izi sizobvuta kwani kwani ngati ife tiri mwa Khristu, yemwe anamenya kale nkondo yotere ndipo anapambana, Iye ndi chitsanzo chathu. Ifenso tikazindikira chinsinsi cha Mau ake, tidzapambana ngati Khristu Yesu. Onani powerenga Aefeso 5:23-32, momwe okhulupirira oyamba akutchulidwira *“mkazi”* ngati kuti popeza anali *“mbeu yeni yeni ya mkazi”*, alinso *“mkazi”* ndipo kuti ifenso lero, tikhoza kukhala mkazi monga Baibulo limanenera ngati tikhulupirira ndi kubatizidwa mwa Yesu.

Mwanjira imene'yi, monga mbeu ya mkazi iyimira Yesu ndi onse omukhulupirira pokhala moyo wao ngati Khristu, koteronso, ana kapena mbeu ya njoka imalankhula ngati njoka (mdierekezi wa m'Baibulo) ndipo imakhalanso umoyo wake ngati wa njoka'yo. Anthu otere, samalabadira kapena kusamala Mau a Mulungu zomwe zidzawatsogoza ku chitonzo cha tchimo ndi kupatulidwa pochotsedwa kwa Mulungu, ngati momwe zinachitikira kwa Adamu ndi Hava. Powona kuti a Yuda ndiamene anapereka Yesu kuimfa – mwachitsanzo, “pobvulaza mbeu ya mkazi pa chidendene”, tiwona kuti iwo anakhala ngati chitsanzo chachikulu cha mbeu ya njoka ija. M'malo mopha Yesu, anangomubvulaza osapheratu ayi. Yohane Mbatizi, akutitsimikizira izi mogwirizana ndi Yesu:-

“...Ndipo iye (Yohane) pakuona ambiri Afarisi ndi Asaduki (gulu la a Yuda lomwe lidanyoza Yesu) akudza ku ubatizo wake, anati kwa iwo, Obadwa (olengedwa, oberekedwa mu utchimo) a njoka inu, ndani anakulangizani kuthawa mkwiyo ulinkudza?...” (Mateyu 3:7).

“...Ndipo Yesu anadziwa maganizo awo (a Afarisi), naati kwa iwo,akubadwa inu a njoka, mungathe bwanji kulankhula zabwino, inu akukhala oyipa?...” (Mateyu 12:25,34).

Dziko lonse, ngakhale dziko la chipembedzo – liri ndi makhaliidwe ndi zizindikiro za njoka. Anthu okhawo omwe anabatizidwa mwa Khristu ndi omwe angakhudzidwe ndi lonjezo la mbeu ya mkazi; ena onse mwanjira za utchimo osiyana siyana, ali mbeu ya njoka (tchimo). Ife lero tiyenera kutsata chitsanzo chabwino cha Yesu Khristu pa zomwe ankachita pokhala pakati pa mbeu ya njoka pa dziko lapansi:-

-Iye analalikira kwa iwo mwa chikondi komanso mokhudzidwa mwapadera m'choonadi ngakhale kuti

-Sanalole makhaliidwe ndi maganizo awo alondolere umoyo Wake ndipo

-Iye anawaonetsa iwo mkhalidwe wa chikondi weni weni wa Mulungu omwe Iye anakhala nawo.

Komabe, ngakhale anakhala choncho, iwo sanamukondebe koma anamudabe. Makhalidwe ake omvera Mulungu anapangitsa kuti iwo asamusangalalire kotero m'malo mwake, anamuchitira kaduka. Ngakhale a m'banja lake amene (Yohane 7:5; Marko 3:21), ndi anzake okonedwa ake omwe (Yohane 6:6), anayesetsa kumutsekereza ndipo mpaka anamuthawa pamabvuto ake omwense m'njira ina, anali mabvuto athu. Paulo naye, anaonanso zinthu ngati zimenezi pamene anadandaula kwa anzake onse omwe masiku oyambirira ankakhala pafupi ndi iye nthawi yambiri mu zobvuta kapena zabwino.

“...kodi ndasanduka m'dani wanu, pakukunenerani zoona?” (Agalatiya 4:14-16).

Choonadi ndi choyipa pakati pa ochimwa, sichinthu chotchuka ayi; pozindikira ndi kukhala m'choonadi nthawi zonse, tidzapeza mabvuto osiyana siyana ndi ena, ndipo zotsatira zake ndi kunzunzidwa kapenanso kuphedwa kumene.:-

“...Komatu monga pompaja iye wobadwa monga mwathupi ananzunza wobadwa monga mwa Mzimu (pozindikira zowona zeni zeni za Mau a Mulungu – 1 Petro 1:23), **momwense tsopano....”** (Agalatiya 4:29).

Tikagwirizana mu umodzi ndi Khristu, tiyenera tilandire chitonzo,tilandire zowawa, kotero tidzagawane mu ulemmero wa Mphatso yake. Panonso Paulo, atikumbutsa popereka chitsanzo chapamwamba za izi:-

“...Okhulupirira Mau'wa: Pakuti ngati tidamwalira ndi Iye, tidzakhalanso ndi moyo ndi Iye ngati tipirira, tidzachitanso (kulamula) **mu Ufumu ndi Iye”** (Khristu); **“Mwaichi, ndipirira zonse”** (2 Timoteo 2:10-12).

“...Ngati anandilonda londa ine (kunzunza), **adzakulonda londani inunso; Koma izi zonse adzakuchitirani chifukwa cha dzina langa..”** (Yohane 15:20,21).

Mwachitsanzo, chifukwa chakuti tinabatizidwa mu dzina la Yesu (Machitidwe 2:38; 8:16).

Kungowerenga ndime zimenezi, tikhoza kuyesedwa poganiza kuti ngati ziri chonchi, kuli bwino kungosiya osakhalanso “mbeu ya mkazi” mwa ubatizo wa

Khristu chifukwa chokana mazonzu'wa. Tiyenera kuzindikira kuti Mulungu amapereka mphamvu zake kwaife mogwirizana ndi mlingo womwe ife tingakwanitse. Pamene kudzipereka m'ntchito ya Khristu n'kofunikira, umodzi wathu ndi Iye udzatiyenera kulanira mphoto kotero “...*mazunzo a nthawi zino sadzafanana ndi chiulemerero chomwe chidzaundukulidwe kwaife*”. Ndipo ngakhale pano, Iye anadzipereka ku nsembe, komanso ngakhale kudzipereka kumeneku kumapangitsa kuti mapemphero athu azimveka mosabvuta panthawi ya mazunzo athu, mapemphero'wa amakhala a mphamvu ndipo amayankhidwa mwamsanga ndi Mulungu ngati ifenso, tikhulupirira modzipereka. Pongwonjezera izi, Abale a Yesu (christadelphians) amapeza chilimbitso chachikulu chochokera m'Baibulo chomwe iwo amawerenga pafupi pafupi:-

“...Koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi chiyeso adzayikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako, ndikuti mudzakwanitse,” (1 Akorinto 10:13).

“...Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukhale nawo mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala nacho chibvuto, koma limbikani mtima; ndalalika (ndipo ndagonjetsa) dziko lapansi Ine. (Yohane 16:33).

“...Ndipo tidzatani ndi zinthu izi? Ngati Mulungu ali ndi ife, adzatikaniza ndani?” (Aroma 8:31).

3.3 MALONJEZANO KWA NOWA

Mopitirira ndi mbiri ya munthu itatha nthawi ya Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni, munthu anapitiriranso mu utchimo. Zinthu zinafika pobvuta pamene chitukuko chinafika padziko, makhalidwe a munthu anawonjezekera kuyipa ndi chikhalidwe chake choncho, Mulungu anaganiza zowononga chikhalidwe choyipa chotere, kupatula banja la Nowa ndi iye mwini banja'lo (Genesis 6:5-8). Iye anamuwuzza Mulungu kuti akonze chombo kotero, Nowa, banja lake ndi mtundu uliwonse wa nyama padziko lapansi ukanakhalamo pa nthawi yonse yomwe madzi anasefukira padziko lonse. Ndipo mbiri ya kale komanso a za

- ◆ **“....chifukwa kuti dziko lonse lapansi lidzadzala ndi odziwa Yehova, monga mdazi odzaza nyanja..”** (Yesaya 11:9; Numeri 14:21) – zobvuta kwambiri kukwaniritsidwa ngati Mulungu alolera kuti dziko lino liwonongedwe monga timamvera. Lonjezo lotere, silinakwaniritsidwe.
- ◆ **“....Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anawumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwachabe; Iye analiwumba akhalemo anthu...”** (Yesaya 45:18). Ngati Mulungu anapanga dziko kenaka n’kuliwonerera kuti liwonongeke, ndiye kuti analilenga chabe, koteri, ntchito yake inalinso chabe ndipo lonjezo limeneri silidzakwaniritsidwanso kuti **“anthu akhalemo”**

Koma kuchokera mu Genesis, Mulungu analonjeza zonse kwa Nowa. Pamene anthu anayambanso kukhala m’dziko latsopano kutatha kusefukira kwa madzi, Nowa anali wa mantha poganiza kuti mwina kungabwerenso chilango china ndi chiwonongeko chinanso choposa chimenechi. Nthawi zonse ikayamba mvula, maganizo a chiwonongeko chosefukira kwa madzi ankamufikira (ife lero sizichitika). Koteri, Mulungu anapanga malonjezano kuti izi sizidzachitikanso:-

“....Ndipo Ine, tawonani, Ine ndikhazikitsa pangano langa pamodzi ndi inu, ndi mbeu zanu pambuyo panu; ndi zamoyo zonse ziri pamodzi ndi inu, zowuluka, ng’ombe ndi zinyama zonse zadziko lapansi, pamodzi ndi inu; zonse zotuluka m’chingalawa zinyama zonse zadziko lapansi: Ndipo ndidzakhazikitsa pangano langa pamodzi ndi inu (kudabwitsa kwa Mulungu popanga malonjezano ndi munthu), zamoyo zonse sizidzamalizidwanso konse ndi madzi a chigumula; ndipo sikudzakhalanso konse chigumula chakuwononga dziko lapansi” (Genesis 9:9-12).

Pangano iri linatsimikizidwa popereka chizindikiro cha Uta wa Leza:

“....Ndipo anati Mulungu, ichi ndi chizindikiro cha pangano langa limene ndipangana ndi Ine ndi inu, ndi za moyo zonse ziri pamodzi ndi inu, ku mibadwo mibadwo; ndiyika Uta –wa-Leza wanga m’mtambomo (wa mvula), ndipo udzakhala chizindikiro cha pangano lopangana ndi Ine ndi dziko lapansi. Ndipo padzakhala

pophimba ndi mitambo Ine dziko lapansi, utawo udzawoneka m'mitambomo; ndipo ndidzakumbukira pangano langa limene ndi Ine ndi inu, ndi zamoyo zonse zokhala ndi moyo; ndipo madzi sadzakhhalanso konse chigumula chakuwononga za moyo zonse. Ndipo utawo udzakhala m'mtambo; ndipo ndidzayang'anira kuti ndi kumbukire pangano la chikhalire liri ndi Mulungu ndi zamoyo zone zokhala ndi moyo padziko lapansi. Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, Ichi ndicho chizindikiro cha pangano ndalikhazikitsa popangana ndi Ine ndi za moyo zonse za pa dziko lapansi..."
(Genesis 9:12-17).

Chifukwa chakuti awa ndi malonjezano osatha, a muyaya pakati pa Mulungu ndi anthu komanso nyama zonse padziko lapansi, tiwona kuti n'koyenera kuti nyamazo ndi anthuwo ayenera kukhala m'dziko lapansi kwa muyaya ndi kosalekeza monga panganolo linakhazikidwira. Ichi ndi chitsimikizo chokwanira kuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwadi pa dziko lapanso lino osati kumwamba monga amanenera ena ayi.

Kotero, lonjezano la Mulungu kwa Nowa ndi maziko eni eni a Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu; lonjezo'li likuwonetsa momwe Mulungu amayang'anira dziko lonse lapansi ndiponso momwe Iye afunira kukwaniritsira cholinga chake polenga dziko. Ngakhale pa zobvuta, mazunzo kapena madyerero, Iye amatikumbukira ndi chisomo chake, pa mkwiyo, atikumbukira ndi chifundo (Habakuk 3:2); ndipo ichi ndi chikondi chake chomwe amasamalira anthu ake ngakhale nsomo nyama zake zonse (1 Akorinto 9:9 cp. Yona 4:11).

3.4 MALONJEZANO KWA ABRAHAMU

Uthenga Wabwino womwe Yesu ndi akuphunzira ake anaphunzitsa siunali osiyana ndi Mau a Mulungu omwe Abrahamu anawadziwa. Mulungu kudzera m'Mau Ake "...*anayamba kale kulalikira Uthenga Wabwino kwa Abrahamu...*" Agalatiya 3:8). Mfundo iyi ya malonjezano ndi yofunikira kwambiri kotero, Petro anatimikizira kufunikira kopambana pofotokozerwa za Uthenga Wabwino koyambirira mpaka komalizira kwa ulaliki wake

(Machitidwe 3:13,25). Ngati tingamvetse bwino zomwe Abrahamu anaphunzitsidwa, ndiye kuti tidzakhala ndi chithunzi thunzi chabwino cha Uthenga Wabwino wa chi khristu. Pali zizindikiro zambiri zowonetsa kuti Uthenga Wabwino siwunayambe kuphunzitsidwa nthawi ya Yesu Khristu:-

“....Ndipo ife lero tikulalikirani inu Uthenga Wabwino wa malonjezano ochitidwa kwa makolo athu; (a chi Yuda) kuti Mulungu analikwaniritsa ili kwa ana athu”
(Machitidwe13:32,33).

“....Uthenga Wabwino wa Mulungu umene Iye analonjeza kale ndi mau a aneneri ake (monga Abrahamu – Genesis 20:7) m'malembo Oyera....” (Aroma 1:1,2).

“....chifukwa chaichi, walalikidwa Uthenga Wabwino kwa iwonso adafawo, kuti akaweruzidwe....” (1 Petro 4:6) – mwachitsanzo, wokhulupirira amene adafa ndipo anali moyo mzirumika zoyambirirazo.

“....Pakuti kwa ifenso walalikidwa Uthenga Wabwino, monganso kwa iwo; (Ahebri : 4:2) - mwachitsanzo, ana a Israeli m'chipululu muja.

Tiwona kuti malonjezano kwa Abrahamu ali ndi mfundo zofunikira ziwiri:-

- (1) Zinthu zokhudza mwana wa Abrahamu (Mwana wake wapadera) ndinso
- (2) Zinthu zokhudza dziko kapena malonjezano omwe Mulungu anamulonjeza Abrahamu.

Malonjezano onsewa anakambidwapo m'Chipangano Chatsopano, ndipo mogwirizana ndi maganizo athu ofuna kuti tipeze chilangizo m'Baibulo, tiphatikiza zipangano zonse ziwiri (Chatsopano ndi Chakale); pofuna kuwonetsa momveka bwino chithunzi thunzi chokwanira cha pangano lomwe Mulungu anapanga ndi Abrahamu.

Abrahamu koyambirira an'kakhala ku dziko lomwe tsopano limatchedwa Iraq mu mzinda wotchedwa Ur. Anzathu ofufuza fufuza pokumba pansu

anawonetsa kuti malo amene'wa adali malo a chitukuko choposa pa nthawi yomwe Abrahamu ankakhalako. Kunali kale malo osungirako ndalama (ma banki), anthu ogwira ntchito m'bama ndi zomanga zosiyana siyana. Mwachikhalidwe chawo, anthu onse kuphatikizapo Abrahamu, ankakhala mu mzinda umene'wu; monga tidziwa anakhala umoyo wake onse ngati momwe anthu ena onse amakhala mu mzindawo. Munthu wa dziko lapansi wokhala m'malo a chitukuko, malo a zochita zosiyana siyana monga uchimo ndi chiyero, zoyipa ndi zabwino. Komabe, nthawi inafika pamene Abrahamu anayitanidwa ndi Mulungu – kuchoka mu Mzinda wa Ur, kusiya umoyo wa pamwambawo kuti apite pa ulendo wa ku dziko la malonjezano. Panthawi'yi Abrahamu sankadziwa komwe anawuzidwa komanso kukopeka kupitako. Monga anawuzidwa ndi Mulungu, kunapezeka kuti ulendo unali wautali pa mtunda wosachepera 1,500 mailosi. Dzikolo linali la Kanani lomwe lero lino limadziwika ndi dzina lakuti “Israeli”.

Pafupi fupi umoyo wake onse, Mulungu ankawonekera kwa Abrahamu kotero, anapitiriza mobwereza bwereza malonjezano ake kwa iye. Malonjezano amenewa ndi amene anatsimikizirapo potsamira kwambiri pa chiphunzitso cha Yesu cha Uthenga Wabwino; choncho, ngati a khristu owona, mayitanidwe a Abrahamu akutifikiranso ife lero monga anamufikira Abrahamu, kuti tichoke naye pamodzi m'mizinda yathu ya zitukuko zosiyana siyana, tisiye zonse zoyipa za moyo uno, n'kuyang'ana patsogolo mu umoyo wa chikhulupiriro, pogwiritsa ntchito malonjezano a Atate wathu mu Mau Ake Oyera. Tiyeni tingoganizira, Abrahamu anasiya zabwino ndi zokoma zonse za mu Mzinda wa Ur, kupita kumalo komwe kudalibe chitukuko china chiri chonse chifukwa cha malonjezano chabe a Mulungu! “...*Ndi chikhulupiriro Abrahamu, poyitanidwa, anamvera kutuluka* (mu Mzinda wa Ur) *kunka ku malo* (ku Kanani) *amene adzalandira ngati cholowa; ndipo anatuluka wosadziwa kumene akamukako....*” (A Hebri 11:8).

Pamene tikuganizira za malonjezano a Mulungu koyamba, ifenso titha kumawona ngati kuti sitikudziwa choyenera kuchita, kuti kapena dziko la malonjezano'lo ndi lotani kapena kuti liri kuti, nanga kuti Ufumu wa Mulungu'wo ndi chiyani ndipo udzakhala wotani. Tiyenera kuzindikira kuti chikhulupiriro chathu mwa Mulungu chiyenera kukhala cha mphamvu ndi changwiro kotero, tikamumvere Mulungu'yo.

Abrahamu koyambirira sanali munthu wongoyenda yenda ngati momwe zinachitikira atawuzidwa kuchoka mu Mzinda wa Ur ayi, koma anali munthu okhazikika m'dziko lake loyamba'lo. Anayamba kuyenda yenda chifukwa cha malonjezano aja pofuna funa moyo wosatha. Makhalidwe ake kotero, sanasiyane konse ndi umoyo wathu wa lero. Anabvutika m'maganizo kusiya zonse zomwe zinali zokoma mu Mzinda wa Ur ndi kutsatira Mulungu pololera kupita ku malo a chilendo, komwe kunali zochitika za chilendonso; monga ife timabvutikira tikayitanidwa ndi Mulungu, timakumana ndi zilankhulo zosiyana ndi zathu, chikhalidwe ndi zochita zosiyana ndi zomwe ife timadziwa; zonsezi Abrahamu anakumana nazo. Tikamawerenga kuti kungowona zomwe anachita Abrahamu pobvomera mayitanidwe ake kwa Mulungu, tiwoneratu kuti Abrahamu analimbikitsidwa ndi Mulungu chifukwa chomvera ndi chikhulupiriro chake. Iye anakhulupirira malonjezano a Mulungu. Ndiyesa kuti an'kaloweza Mau a Mulungu'wa tsiku ndi tsiku nkumawaganizira malonjezano amenewa komanso kumasulira zonsezi mu mtima mwake.

Powonetsa kumvera ndi chikhulupiriro cha mtundu wotere, ifenso tikhoza kulandira ulemu waukulu monga Abrahamu analandira. Ndipo mwaichi, tidzatchedwa abwenzi a Mulungu (Yesaya 41:8), kotero, tidzapeza nzeru mwa Mulungu (Genesis 18:17) ndiponso tidzalandira chiyembekezo cheni cheni cha moyo wosatha mu Ufumu Wake. N'chifukwa chake, Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu unatsamira pa malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu. Tikakhulupirira m'choonadi cha Khristu, ifenso, tiyenera kudziwa kwambiri malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu. Popanda kudziwa malonjezano amenewa, chikhulupiriro chathu chiri chabe. Tiziwerenga kawiri kawiri ndi chidwi chonse, za malonjezano pakati pa Mulungu ndi Abrahamu.

DZIKO

- 1.) ***“...Tuluka iwe m'dziko lako, ndi kwa abale ako.....kunka ku dziko limene ndidzakusonyeza iwe;”*** (Genesis 12:1).
- 2.) Abrahamu ***“....anankabe ulendo wake....ku Beteli*** (Chikatikati cha dziko la Israeli) ***.....Ndipo Yehova anati kwa Abrahamu....Tukula maso ako, nuyang'anire kuyambira kumene uliko, kumpoto, ndi kum'mwera, ndi kum'mawa, ndi kumadzulo: Chifukwa kuti dziko lonse limene ulinkuliwona, ndidzakupatsa iwe ndi mbeu yako nthawi zonse....Tauka, nuyende yende m'dzikoli***

m'litali, mwache ndi m'mimba mwakechifukwa kuti ndidzapatsa iwe limenelo..” (Genesis 13:3,14-17).

- 3.) *Tsiku lomwelo Yehova anapangana chipangano ndi Abrahamu, naati, Ndidzapatsa mbeu zako dziko lapansi ili, kuyambira pa nyanja ya Aigupto kufikira pa nyanja yayikulu, nyanja ya Firate....”* (Genesis 15:18).
- 4.) *“....Pakuti lonjezo lakuti iye (Abrahamu) adzakhala mlowamalo wa mfumu ya dziko lapansi (mfumu)....”* (Aroma 4:13).

Tikuona pano kuti umboni unalalikidwa kwa Abrahamu unali:-

- 1.) “Pali malo kapena titi dziko limene iwe uyenera kupitako”
- 2.) “Wafika tsopano kumalo kuja. Iwe ndi ana ako (mbeu yako) udzakhala kuno nthawi zonse” Onani momwe lonjezo la moyo wosatha walembedwera mosatsindika: Munthu wamba apa akadangolemba zodziwa iye ndi zofuna zake.
- 3.) Malo amalonjezano`wa anali ndipo ndi malo eni eni, sinkhambakamwa chabe ayi.
- 4.) Abrahamu sadayembekezere kulandira lonjezo lake mu umoyo uno kapena kuti pa nthawi imene iye anali moyo m`dziko la Kanani, iye anali “mlendo” m`dzikolo, ngakhale kuti panali chiyembekezo chakuti anayenera kukhala ku maloko nthawi zosatha (muyaya, kosalekeza). Zimenezi zikutanthawuza kuti iye adayenera kufa , kenaka akadawukitsidwa kwa akufa, ndipo powukitsidwa choncho, zikanamuyenereza tsopano kulandira malonjezano ake ndi Mulungu. Nthawi yotere sinamufikire Abrahamu (A Hebri 11:13-24).
- 5.) Paulo, mowumirizidwa ndi mphamvu ya Mulungu, anawona malonjezano kwa Abrahamu atamufikira iye nalandira ndi chisangalalo moyo wake wonse, nakhala m`modzi mwa olamulira dziko lapansi.

Monga tanena kale, Abrahamu sanalandire malonjezano onse pamoyo wake mpaka lero pamene akadali m'manda. Iye akuyembekezerabe kulandira mapangano akadzawukanso kwa akufa:-

“...Ndi chikhulupiriro anakhala mlendo kudziko la malonjezano, losati lake (kuwoneka kuti moyo wake unali moyo ongoyembekezera), **nakkhalira m'mahema pamodzi ndi Isake ndi Yakobo olova m'nyumba pamodzi ndi iye a lonjezano lomwelo....”**
(A Hebr 11:9).

Iye anakhala ngati wobwera m'dzikolo, mwina chifukwa chakuti sanali ndi mganizo oti ankatetezedwa, apa tingati anali chimodzi modzi munthu othawa kwawo chifukwa cha mabvuto ngati a nkhondo kapena za ndale. Sanathe kukhala ndi ana ake m'dziko la kwawo monga Isake ndi Yakobo (omwense anawuzidwanso mobwereza bwereza za malonjezano a Abrahamu ndi Mulungu), iye **“...adamwalira m'chikhulupiriro, osalandira malonjezano, komatu adawaona ndi kuwalandira kutali** (kutsogolo kwa moyo wawo) **nabvomereza kuti ali apanjira ndi aulendo padziko....”** (A Hebr 11:13). Onani kuti pali ndondomeko zinayi:-

- Kudziwa ndi kuzindikira malonjezano – monga tikuchitira panopa powunika Mau a Mulungu mogwirizana ndi zolembedwa m'Baibulo m'maphunziro ano.
- Titakhudzidwa ndi iwo (mau'wo) – ngati zinamutengera nthawi yaitali Abrahamu kuti akhutire Mau a Mulungu, ziri kotani ndi ife lerolino?
- Kunyadira Mau a Mulungu'wo titawamvetsa bwino – pomvera ndi kubatizidwa mwa Yesu Khristu (Agalatiya 3:27-29).
- Kulapa pochitira umboni ku dziko lonse lapansi powonetsa mu umoyo wathu wa lero kuti m'dziko tirilimu, ndife aulendo kotero, tikukhala m'chiyembekezo cha dziko lokoma lirin'kudzalo.

Abrahamu angakhale chitsanzo chatu chonyaditsa tikalola ndi kukhudzidwa ndi zinthu tawerenga'zi. Tikangodziwa kuti malonjezano onse a Mulungu agonera pa chikhulupiriro ndi kuzindikira kwa Abrahamu, tidzakhutitsidwa ndi kuzindikira koposa cholinga cha Mulungu paife ndi dziko lapansi; Abrahamu

anadziwa izi kotero anagula mbali ina ya dziko la malonjezanolo pofuna kutsimikizira kuti ndi dziko lakedi pamene anayika m'manda mkazi wake Sarah (Machitidwe 7:17). Zoonadi, Mulungu “...*ndipo sanampatsa cholowa chake* (inheritance?) *m'menemo, ngakhale popondapo phazi lake iai; ndipo anamlonjezera iye kuti adzampatsa ili, likhale lake, ndi la mbeu yake yom'tsatira angakhale analibe mwana pamenepo...*” (Machitidwe 7:5). Ndikhulupirira kuti mbeu ya masiku ano ya Abrahamu ikhozanso kuganiza kuti ikagula kapena kubwereka malo lero padziko lino, ndiye kuti afikapo komanso kuti angakwaniritse zomwe Abrahamu anachita, koma tisayiwale kuti Iye ndi Mulungu, ndi chikhulupiriro mzonse zomwe Mulunguyo amatipatsa monga Abrahamu anawuzidwa, ife tidzapindula.

Kotero, tidziwensola kuti zoona, Mulungu amasunga malonjezano Ake. Panopa, tikudikira tsiku limene Abrahamu atate wathu, ndi ena onse omwe analonjezedwa ndi Mulungu, kuti adzalandire malonjezano awo ndi chisangalalo Yesu akadzabweranso panso pano. Paulo pa AHebri 11:13,39,40 akutitsimikizira mfundo imeneyi yokama'yi motere:

“...Iwo onse adamwalira m'chikhulupiriro, osalandira malonjezano,popeza Mulungu adatikonzera ife kanthu koposa, kuti iwo asayesedwe a mphumphu opanda ife...” (A Hebri 11:13,39,40).

Onse okhulupirira m'choonadi choncho, adzapatsidwa mphotho pa nthawi yomweyo, mwachitsanzo, panthawi ya chiweruzo yomwe ndi tsiku lomaliza (2 Timoteo 4:1,8; Mateyu 25:31-34; 1Petro 5:4). Kuti zidzatheke pofuna kuweruzidwa patsikuli, Abrahamu ndi ena onse akufa mu nzeru zawo, omwensola ankadziwa za malonjezano'wo, onse adzawukitsidwa nthawi'yo itayandikira. Ngati lero anthu onsewa sanalandirebe malonjezano'wa, ndipo kuti adzalandira mapangano'wo akadzawukanso kwa akufa patsiku la chiweruzo pamene Yesu adzabweranso, ndiye kuti palibe njira inanso koma kulola kuti onse akufa Abrahamu, sazindikira chomwe chikuchitika lero padziko, iwo saalinsola ndi moyo monga ena amanenera, mpaka Yesu akadzabwera; Kotero, nkulakwitsa kunena kuti Abrahamu ali ndi moyo kumwamba pamene Baibulo lomwe linalembedwa zaka zambiri Abrahamu atafa kale, limaneneratu kuti Abrahamu'yo adzakhala ndi moyo tsiku lomwe adzawukitsidwe'lo. Ena ambiri padziko lapansi amakhulupirira kuti Abrahamu ali ndi moyo, ndizomvetsa chisoni kwambiri kuti izi siziri choncho ndipo

mwadziwerengera nokha kuti iri ndi bodza lomwe lija la m'munda wa Eden. Kodi inu mukulolera kuti musiye zoonadi zeni zeni monga mwawerenga m'Baibulo n'kutsata ulaliki wabodza wotere?

MBEU

Monga tanena m'Phunziro 3:2, lonjezano la mbeu likukhudza kwambiri choyamba kubadwa kwa Yesu ndiponso kachiwiri, kubadwa kwa iwo onse omwe ali "mwa Yesu Khristu" choncho, akuwerengedwanso ngati mbeu ya Abrahamu:-

1. *"....ndipo ndidzakupanga iwe kukhala mtundu waukulu, ndipo ndidzakudalitsa iwe ... ndipo mwa ine adzadalitsika mabanja onse a dziko lapansi"* (Genesis 12:2,3).
2. *"....chifukwa kuti dziko lonse limene ulinkuliona, ndidzakupatsa iwe ndi mbeu yako nthawi zosatha. Ndipo ndidzayesa mbeu yako monga mfumbi lapansi: chotere kuti ngati munthu angathe kuwerenga mfumbi lapansi, chomwechonso mbeu yako idzawerengedwa....."* (Genesis 13:15,16).
3. *"....Tayang'anatu kumwamba, uwerenge nyenyezi, ngati ukhoza kuziwerenga zimenezo:....Zoterezo zidzakhala mbeu zako.Ndidzapatsa mbeu zako dziko ili, kuyambira pa nyanja ya Aigupto kufikira pa nyanja yaikulu...."* (Genesis 15:5,18).
4. *"....Ndidzakupatsa iwendi mbeu yako ya pambuyo pako....dziko lonse la Kanani likhale lako nthawi zosatha ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wao...."* (Genesis 17:8).
5. *"....ndidzachelukitsa mbeu zako monga nyenyezi zakumwamba, monga mchenga wa m'mpheapete mwa nyanja; ndipo mbeu zako zidzagonjetsa chipata cha adani awo; m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa; chifukwa wamvera Mau anga...."*(Genesis 22:17,18).

Tidziwenso pano kuti, Abrahamu adaziwiratu kuti mbeu ikukambidwa apayi ndi mbeu yake koma yodzabadwa m'mibadwo yakutsogolo kwa moyo wake kudzera mwa ana ake:-

1. Choyamba iye anangowuzidwa kuti mwanjira ina yake adzakhala ndi ana ambiri, ndiponso kuti kudzera mwa m'modzi mwa ana (mbeu yake) ake, mtundu wonse padziko lapansi udzadalitsika.
2. Kenaka, anawuzidwanso kuti adzakhala ndi mbeu yomwe ikukambidwa pophatikizanso anthu ena ambiri. Anthu amenewa, akanadzakhala mu umoyo wamuyaya pamodzi ndi Abrahamu'yo mudziko limene iye anali kupondamo pa nthawi'yo, mwa chitsanzo, Kanani.
3. Anawuzidwanso kuti mbeu yake ikanadzakhala yochuluka kwambiri monga momwe nyenyezi zirili mlengalenga. Apa ndikhulupirira kuti anaganizirapo zoti adzakhala ndi ana m'chipembedzo chake (ana obadwa mu uzimu osati mu thupi ayi), omutsatira iye popembedza Mulungu wake woona'yo (ngati nyenyezi za mlengalenga); pamwamba pa apo ana ake eni eni a chibadidwe (monga "mchenga wa pa dziko lapansi").
4. Malonjezano a m'mbuyomu, anatsimikizidwa ponena motsindika, kuti anthu ambiri omwe adzakhale nawo pamodzi ngati "mbeu'yo" adzayenera kukhala odzipereka mwapadera pa ntchito ya Mulungu ndinso kukhala pafupi ndi Iye.

Zindikirani kuti mbeu ija idayenera kubweretsa "madalitso" kwa anthu a m'dziko lonse lapansi. M'Baibulo, tikaganiza za madalitso, timalumikizanso maganizo amene'wa ndi chikhululukiro cha machimo. Ndipo ili ndi dalitso lalikulu zedi lomwe munthu aliyense okonda Mulungu akhoza kusangalala nalo. N'chifukwa chake timawerenga *"...wodala munthu'yo wokhulukidwa tchimo lake; wokwiridwa choyipa chake..."* (Masalmo 32:1); *"chikho cha dalitso..."* (1 Akorinto 10:16), ponena za chikho cha

vinyo chomwe chimayimira mwazi wa Khristu, womwe ife tikamwa, umatisendeza ku chikhululukiro cha tchimo poganizira patokha molapa, mazunzo a Khristu.

Mbeu yokhayo ya Abrahamu yomwe inabweretsa chikhululukiro cha machimo padziko lino lapansi ndi Yesu Khristu yekha, ndipo Chipangano Chatsopano chimathirira ndemanga pa malonjezano kwa Abrahamu koteru, ichi ndi chitsimikizo kuti palibe kusiyana pakati pa Chipangano Chatsopano ndi Chakale:-

“...Mulungu ndipo sanati, ‘ndipo zimbeu,’ ngati kunena zambiri (mwachitsanzo, ngati mbeu zambiri kapena ana ake ambiri) komatu kwa mbeu yako, ngati kunena imodzi, Ndipo kwa mbeu yako ndiye Khristu....” (Agalatiya 3:16).

“...Inu ndinu ana a aneneri, ndi a panganolo Mulungu anapangana ndi makolo anu, ndi kunena kwa Abrahamu, Ndipo mu mbeu yako mafuko onse a dziko adzadalitsidwa. Kuyambira ndi inu, Mulungu, atawukitsa Mwana Wake Yesu (mwachitsanzo, mbeu yake kapena Mwana wake wa Abrahamu!) anamtuma kukudalitsani inu, ndi kukubwezani yense ku zoyipa zake....” (Machitidwe 3:25,26).

Imvani tsopano momwe Petro akufotokozera m’nkhani yopezeka pa ndime ya Genesis 22:18 m’munsimu omwe awonetsedwa ngati masamu:-

Mbeu = Yesu (zonse ndi zofanana m’Baibulo)

Dalitso = Chikhululukiro cha machimo (zonse ndi zofanana m’Baibulo M’matanthawuzo ake ngati momwe zinalembedwera)

Lonjezo lonena kuti Yesu, mbeu’yo akanagonjetsa adani ake, tsopano likugwirana bwino tikawona ndi kulingalira zomwe Yesu anachita makamaka tikawerenga zonsezi, mogwirizana ndi momwe Iye anagonjetsera tchimo – mdani wamkulu wa anthu a Mulungu, choncho, Yesu naye ndi mdani wakenso Wamkulu.

Panopa, tsopano ndi zomvekadi kuti chikhulupiriro cha a khristu cha Uthenga Wabwino, chinali chodziwika kwambiri kwa Abrahamu. Koma malonjezano ofunikira otere kwa Abrahamu ndi mbeu yake Yesu, inalinso yofunikira. Nanga ena onse ofunikira sakanatha kukhala mbeu? Nanga iwo anatani kukhalanso mbeu? Ngakhale anthu obadwa mwa Abrahamu (Ishimaeli) sakanatha kukhala m' modzi mwa wotchedwa dzina loti "mbeu" (Yohane 8:39; Aroma 9:7). Mwanjira ina yake, ife tiyenera kukhala pamodzi ndi Yesu kotero, malonjezano kwa mbeu ija anapangidwanso kwa ife ngati tikhulupirira. Izi zingatheke ngati ife tibatzidwa mwa Yesu (Aroma 6:3-5); Kawiri kawiri, timawerenga kuti ubatizo m' dzina la Yesu Khristu ndi wofunikira (Machitidwe 2:38; 8:16; 10:48; 19:5). Agalatiya 3:27-29 sakuchitira mwina koma kufotokoza momveka bwino pa mfundoyi:-

"...Pakuti nonse amene munabatizidwa mwa Khristu mudabvala Khristu. Muno mulibe Myuda, kapena Mherene (amitundu) , muno mulibe kapolo, kapena a mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi; pakuti muli nonse m' modzi mwa Khristu Yesu. Koma ngati muli a Khristu (mu ubatizo), muli mbeu ya Abrahamu, nyumba monga mwa lonjezano".

Tiona tsopano kuti moyo wosatha udzakhala padziko lapansi, polandira "madalitso a chikhululukiro cha machimo kudzera mwa Yesu Khristu. Ndiubatizo wokha mwa Khristu, Mbeu, omwe umatipatsa ife mwayi wogawana nawo malonjezano omwe ananedwa (za Iye) kwa Abrahamu kholo'lo. Aroma 8:17 akutchula ife okhulupirira "ana a Chifumu ndi Khristu".

Kumbukirani kuti dalitso'li linafikira kwa anthu onse m' dziko lonse lapansi kudzera mwa mbeu; ndipo kuti mbeu'yo idayenera kukhala anthu ambiri m' dziko lonse lapansi, monga m' chenga wa m' mphepete mwa nyanja ndinso monga nyenyezi za mlengalenga. Tidziwanso kuti izi zidzatheka anthu'wo akad zamvera nalandira madalitso kotero, athe kukhala amodzi a mbeu'yo. Choncho, liwu limodzilo lidzadziwika ndi Mulungu Ambuye'yo poyimira anthu ambiri'wo (unyingi wa anthu; Masalmo 22:30). Tikhoza kufotokoza mwachidule za malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu m' magawo awiri motere:-

(1) **-DZIKO**

Abrahamu ndi mbeu yake, Yesu, ndi ena onse amene ali mwa Khristu adzalandira dziko la Kanani ndipo powunikiridwa m'chiphiphiritso, dziko lonse lapansi, ndikuti adzakhalamo nthawi zosatha. Mu umoyo uno, anthu sangathe kulandira chikwaniritso cha malonjezano'wa ndipo kotero, adzalandira pa tsiku lomaliza, Yesu akadzabweranso padziko lapansi.

(2) **-MBEU**

Iyi koyambirira inkayimira Yesu. Kudzera mwa Iye, machimo (“machimo” [“adani”]) a anthu, adzagonjetsedwa, kotero, madalitso a chikhululukiro cha machimo adzakhalapo pa dziko lonse lapansi.

Mu ubatizo m'dzina la Yesu Khristu, timakhala mbali imodzi ya mbeu.

Magawo awiri amenewa, akuwonekanso mu maulaliki a Chipangano Chatsopano, ndinso kuti ataphunzitsidwa, anthu nthawi'yo podziwa, anabatizidwa. Iyi inali, ndipo iri njira yokhayo yomwe malonjezano'wo anapangidwira kwaife. Zonsezi zikutizindikiritsa chifukwa cheni cheni chimene Paulo ngakhale anali munthu okalamba, atayandikira imfa, anakwanitsa kufotokozera mwachimvekere za chiyembekezo chake kuti chinali **“Chiyembekezo cha (mfuko la) Israeli”** (Machitidwe 28:20): Chiyembekezo choonadi cha chikhristu ndichiyembekezo choyambirira cha chi Yuda. Ndemanga ya Khristu kuti **“...chipulumutso ndi cha a Yuda”** (Yohane 4:22) chikutitsimikizira kufunika kwake kwa ife kukhala ndi umoyo wa chipembedzo cha chi Yuda, kotero ife tikapindule nawo m'malonjezano a chipulumutso mwa Khristu, omwe anapangidwa kwa makolo athu (Abrahamu, Davide ndi ena otero) a chi Yuda:

Tiwerenga kuti a khristu anzathu oyambirira anali:-

1.) **“...kulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu**

ndi

- 2.) **“...dzina la Yesu Khristu”** (Machitidwe 8:12).

Izi ndi zinthu ziwiri zomwe zinalongosoledwa kwa Abrahamu m’mitu yosiyanyirirapo:

- 1.) **Analonjezedwa za malo a dziko** ndi
 2.) **Malonjezano okhudza mbeu**

Onani kuti **“zinthu”** (zambiri) zokhudza Ufumu ndi Yesu zakambidwa mwachidule ngati “kulalikira Khristu” (Machitidwe 8:5 cp ndime 12). Nthawi zambiri izi zimatanthawuza kuti “Yesu amatikonda! Mukangonena kuti Iye anafa chifukwa chaife, ndipo kuti inu ndi ife tonse ndife opulumutsidwa!” Ndiye kuti pali chikondi ndi chiyembekezo cha zabwino kwa okhulupirira onse. Koteronso, mau oti “Khristu” akuwonekeratu pawokha kuti mwachidule, amaphunzitsa zinthu zingapo zokhudza Iye ndinso kubwera kwake komanso kwa Ufumu wa Mulungu padziko lapansi. Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu omwe unalalikidwa kwa Abrahamu ndi umene watenga mbali yaikulu pa ulaliki ndi mafalitsidwe a Uthenga Wabwino’wu.

Pamene Paulo anali ku Akorinto, **“...ananena molimba mtima miyezi itatu, natsutsana ndi kuopa kunena ‘za Ufumu wa Mulungu’...”** (Machitidwe 19:8); Ku Aefeso, anayenda malo onse “kulalikira Ufumu wa Mulungu” (Machitidwe 20:25), ndipo kwa Aroma (Rome) nyimbo yake idali yomweyi, **“awafotokozera, ndi kuchitira umboni Ufumu wa Mulungu, ndi kuwakopa za Yesu,...zochokera m’chilamulo cha Mose ndi mwa aneneri,...wosamletsa munthu,”**(Machitidwe 28:23,31). Monga tawona kuti panali zambiri zoyenera kulankhulidwa, kulalikira ndi kufalitsa uthengawu, ichi chititsimikizira kuti Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi Yesu Khristu, siudali wongonena kuti “khulupirirani Yesu” ayi. Unkawoneka ndi ntchito zake zabwino nthawi zonse. Chibvumbulutso cha Mulungu kwa Abrahamu chinali chokwanira komanso chomveka bwino m’zinthu zonse za malonjezano kwa iye, ndipo apa ndi pamene pagona chi khristu cheni cheni cha Uthenga Wabwino.

Tawona kuti ubatizo mwa Yesu Khristu umatipanga ife kukhala mbali ya chiwalo kapena tinene kuti mbali imodzi ya chiwalo cha mbeu, choncho, tingathe kulandirapo gawo lina la malonjezanowo (Agalatiya 3:27-29); koma

tidziwenso kuti ubatizo pawokha siwokwanira kutipezetsa lonjezo la chipulumutso. Tiyenera kukhala m'njira ya mbeu, mwa Khristu, ngati ife tifunadi kulandira nawo malonjezano omwe anapangidwa kwa mbeu'yo. Ubatizo kotero, ndi chiyambi; apa ndiye kuti talowa mu mpikisano omwe ufunikira kuthamanga kwambiri kuti tipeze nawonso mphotho'yo. Tidziwe kuti kukhala mbeu ya Abrahamu kokha sindiye kuti takhala kale oyenera pamaso pa Mulungu. Mfuko lonse la Israeli ndi ana eni eni a Abrahamu m'njira ina, koma sizitanhawuza kuti mfuko lonse la dziko la Israeli lidzapulumutsidwa chifukwa chakuti tate wawo ndi Abrahamu ayi. Iwo adzapulumutsidwa pokha pokha atabatizidwa, nakhala umoyo wa chiyero pamaso pa Mulungu monga kholo lawo Abrahamu anachitira (Arom 9:7,8; 4:13,14). Yesu ngati mwana wa Abrahamu anachitanso monga kholo lake anachitira ndipo anawafotokozera a Yuda, **“...Ndidziwa kuti muli mbeu ya Abrahamu; koma mufuna kundipha Ine, chifukwa mau alibe malo mwa inu. Ngati muli ana a Abrahamu, mukadachita ntchito za Abrahamu....”** (Yohane 8:37,39), zomwe zikutanthawuza kukhala umoyo wa chikhulupiriro mwa Mulungu ndi Khristu, Yemwe ndi Mbeu ya malonjezano opangidwa kwa Abrahamu ndinso monga Abrahamu'yo, anakhulupirira malonjezano a Mulungu'wo. (Yohane 6:29).

Tanena kale kuti “mbeu” iriyonse, iyenera kukhala ndi kuwonetsa chikhalidwe chofanana ndi kholo la mbeu'yo. Ngati ife tiridi mbeu yeni yeni ya Abrahamu m'chikhulupiriro, tiyenera kukhala ndi kunyezimira chikhulupiriro ndi chikhalidwe cheni cheni cha m'malonjezano a Abrahamu, osati pongobatizidwa kokha ayi. Ndichifukwa chake, iye atchulidwa **“....kholo la onse akukhulupirira, angakhale iwo sanadulidwa....iwo amene atsata mayendedwe a chilungamo m'chikhulupiriro chija cha kholo lathu Abrahamu chimene iye anali nacho....”** (Aroma 4:11,12). **“....chotero, zindikirani kuti iwo a chikhulupiriro** (mwachitsanzo, mu mtima) **ndiwo ana a Abrahamu....”** (Agalatiya 3:7).

Chikhulupiriro cheni cheni mwa Khristu, chimawonekera mu ntchito zathu pamaso pa Mulungu, kotero ngati izi zisoweka, ndiye kuti sichikhulupiriro choyenera (Yakobo 2:17). Ife timawonetsa chikhulupiriro m'malonjezano'wa monga taphunzira pobatizidwa, kotero, malonjezano'wo amakhala ngati gawo limodzi la umoyo wathu (Agalatiya 3:27-29). Choncho, kodi inu mumakhulupiriradi malonjezano a Mulungu? Iri ndi mfunso limene nthawi zonse tiyenera kumadzifunsa m'miyoyo yathu.

CHIPANGANO CHATSOPANO NDI CHAKALE

Ziyenera kukhala zowonekeratu tsopano kuti malonjezano kwa Abrahamu ndi chifupikitso cha Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Mbali ina yaikulu ya malonjezano omwe Mulungu anapangana ndi a Yuda anali okhudza malamulo a Mose. Malamulo'wa ankafotokozera kuti ngati a Yuda atamvera malamulo a Mose, ndiye kuti adzadalitsika m'moyo wawo wa thupi (Deuteronomo 28). M'malonjezano a mtundu wotere, padalibe lonjezo lokhudza kulandira moyo wosatha m'malonjezano'wo kapena "chipangano". Moteronso, tiwoneratu kuti pali zipangano ziwiri zomwe zidapangidwa:

- 1) Kwa Abrahamu ndi mbeu yake, kulonjezedwa kwa chikhululukiro cha machimo ndi moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu Yesu Khristu akadzabweranso. Lonjezo iri linapangidwa m'munda wa Edeni ndinso kwa Davide.
- 2) Kwa a Yuda mu nthawi ya Mose, powalonjeza mtendere ndi chisangalalo m'moyo uno wa thupi ngati iwo atamvera malamulo omwe anapatsidwa kwa Mose ndi Mulungu.

Mulungu analonjeza chikhululukiro cha machimo ndi mphotho ya moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu, koma izi zinali zotheka chifukwa cha kudzipereka kwa Yesu ngati nsembe ya ulere. Pachifukwa ichi, timawerenga kuti imfa ya Khristu pa mtanda inatsimikizira kukwaniritsidwa kwa malonjezano a mbeu ya mkazi omwe anapangidwa kwa Adamu, ndipo anabwerezedwa kwa Abrahamu (Agalatiya 3:17; Aroma 15:8; Danieli 9:27; 2 Akorinto 1:20); Choncho, mwazi umatchedwa "*mwazi wa mapangano atsopano*" (Chipangano, Mateyu 26:28). Tikumbukire kuti kawiri kawiri Yesu anatiwuzwa kuti tiyenera kumwa chikho cha vinyo nthawi ndi nthawi, chomwe ndi chifukwa chakuti chikuyimira magari ake okhetsedwa panthawi yopachikidwa kwa Iye, kotero, kumwa vinyo kumatikumbutsa zinthu zimenezi (werengani 1 Akorinto 11:25); "*....chikho ichi ndi pangano latsopano* (lonjezo) *m'mwazi wanga wothiridwa....*" (Luka 22:20). Kumwa mwazi wake (vinyo) ndi kudya thupi lake (mkate) zitanthawuza kuti ife tiyenera kubvomereza kukonzekera kulandira zowawa zonse (ngakhale kuphedwa kumene) pofuna kuchita ndinso kukwaniritsa chifuniro cha Mulungu monga

Khristu anachita modzipereka. “Kudya mkate” mosazindikira chikumbutso cha Yesu Khristu ndi ntchito yake ndi chinthu chopanda tanthawuzo.

Nzeru ya Yesu inatitsogolera ife ku chikhululukiro cha machimo ndi ku moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu; kotero, Iye anatitsimikizira za malonjezano opangidwa ndi Mulungu Yehova kwa tate wathu Abrahamu kukhala malonjezano eni eni; Iye anali **“chikole cha nkhoswe ya pangano labwino lopera”** (A Hebrei 7:22). Mu A Hebrei 10:9, Paulo akukamba za Yesu wochotsa **“...choyambacho** (Chipangano), **kuti akayike chachiwiricho...**” (ndime 9,10). Izi zikuwonetsa kuti pamene Yesu anatitsimikizira malonjezano a kwa Abrahamu, Iye anathana ndi Chipangano Choyamba (Chakale), chomwe chinaperekedwa kudzera mwa Mose. Ndime zomwezi zawonetsanso kuti Yesu anakwaniritsa zonsezi mwa imfa Yake pamtanda paja, kotero, imfa’yo isanafike, padali Chipangano Chakale chomwe Iye tsopano anathana nacho (A Hebrei 8:13).

Nkhani’yi, ikutitsimikizira kuti ngakhale Chipangano cholozera za Yesu chinapangidwa koyambirira, chinali chisanakwaniritsidwe mpaka pamene Yesu anafa, kotero, kukwaniritsidwa kwa Chipangano Chakale’cho kukutchedwa **“Chipangano Chatsopano”**. Cholinga cha Chipangano Chakale chinali kulosera zakutsogolo, zimene Yesu akanadzazichita komanso kutsindika kufunikira kwa chikhulupiriro m’malonjezano okhudza Khristu (A Galatiya 3:19,21). Tikawonetsetsa chikhulupiriro mwa Khristu chinatsimikizira choonadi chopezekanso m’malamulo opatsidwa kwa Mose (3:31). Paulo akuyifupikitsa nkhan’yi motere: **“...Momwemo chilamulo chidakhala namkungwi** (mlangizi) **wathu wakutifikitsa kwa Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiriro...**” (A Galatiya 3:24). Mwaichi, chilamulo mwa Mose chinasungidwa ndipo chikusungidwa komanso ndi chopindulitsa kuchiphunzira mpaka lero.

Zinthu zonsezi, sichinthu chapafupi kuzimvetsetsa munthu akangowerenga koyamba; Tiyeni tifupikitse nkhan’yi motere:

- Malonjezano a Mulungu okhudza Khristu anapangidwa kwa a Abrahamu – Chipangano Chatsopano.

- Malonjezano a Mulungu opangidwa ndi Mulungu kwa ana a Israeli okhudza chilamulo chopatsidwa kwa Mose – Chipangano Chakale.
- Imfa ya Khristu. Kutha kwa Chipangano Chakale (2 Akorinto 2:14-17). Kuyamba kwa Chipangano Chatsopano.

Chifukwa chaichi, zinthu ngati kupereka za chithokozi (tithes), kusunga tsiku la sabata ndi zina zotero zimene zidali mbali imodzi ya chilamulo m'Chipangano Chakale, sizinthu zofunikira kweni kweni pa chipulumutso cha munthu – onani Phunziro 9.5. Chipangano Chatsopano chidzapangidwa kwa m'badwo wa Israeli iwo akadzalapa kwathunthu ndinso akadzabvomereza Yesu Khristu (Yeremiya 31: 31,32; Aroma 9:26,27; Ezekieli 16:62; 37:26), ngakhale kuti m'Yuda wina aliyense amene anachita ichi tsopano ndi kubatizidwa mwa Yesu, athanso kulowa nawo mu Chipangano Chatsopano (momwe simumakhala kusiyantsa pakati pa m'Yuda ndi wa mitundu – Agalatiya 3:27-29).

Tikalola ndi kubvomereza izi mowona mopanda chinyengo, chikhulupiriro chotero chidzatipanga ife kukhala odalirika pamaso pa Mulungu komanso oyenera kulandira nawo malonjezano'wo. Anthu kalelo, ankadzudzula a khristu anzathu oyambirira kuti ulaliki wao siudali opindulitsa. Paulo poyankha anawauza kuti chifukwa chakuti chitsimikizo chochokera kwa Yehova Mulungu chinatsimikizidwa mwa malonjezano ake mu imfa ya Khristu, chiyembekezo chimene iwo anakambacho, sichidali chongoganizira kapena kungochipeza monga iwo ankanenera ayi, koma kuti ndi chiyembekezo cheni cheni chotsamira pa ntchito zathu: *“....Pamenepo, pakufuna chimene, kodi ndinachitapo kosintha sintha? Kapena zimene nditsimikizira mtima kodi nditsimikiza mtima monga mwa thupi? Kuti paine pakhale eya, eya ndi iai, iai? Koma Mulungu ali wokhulupirira, kuti mau athu kwa inu sanakhala eya ndi iai. Pakuti mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, amene analalidwa mwa inu ndi ife* (ine ndi Silvano ndi Timoteo) *sanakhala eya ndi iai, koma anakhala eya mwa Iye. Pakuti monga mawerengedwe a malonjezano a Mulungu ali mwa Iye eya; chifukwa chakenso ali mwa Iye Amen,”* (2 Akorinto 1:17-20).

Zoona ndithu, izi zikutsutsiratu maganizo oti *“inde, ndiganiza kuti zikhoza kukhala zowona mukunenazo”* ayi koma kudzitsimikizira tokha m'Buku Lopatulika.

3.5 MALONJEZANO KWA DAVIDE

Davide, monganso Abrahamu ndi ena onse omwe analandira malonjezano a Mulungu, anakhala m'miyoyo yawo mobvutikira. Iye anakula kuchokera m'banja la anthu ambiri ndipo anali mwana womaliza m'banja'li, lomwe nthawi imeneyo mabanja a mfuko la Israeli mzaka 1,000 B.C., zinkatanthawuza kusaka nkhosa komanso kumvera ndi kuchita zofuna za achibale ake omwe anali akulu akulu kwa iye (1 Samueli 15-17). Nthawi imeneyi, ndipamene anaphunzira mlingo wa chikhulupiro mwa Mulungu wake omwe ngakhale ife sitingafikepo lero lino.

Inafika nthawi yomwe Israeli ankawopsyezedwa ndi adani awo monga Afilisiti; adani awo'wa ankawauziratu poyera kuti palibe yemwe angagonjetse Goliyati m'dindoyo, katakwe wa Afilisiti; izi zinkatanthawuza kuti aliyense yemwe akadagonjetsa katswiri wa Afilisiti'yu akanalamulira onse ogonjetsedwa'wo. Mothandizidwa ndi Yehova Mulungu wake, Davide anagonjetsa Goliyati pogwiritsa ntchito legeni (ulaya), kotero, Davide anatchuka kwambiri kuposa mfumu yawo Sauli. *"...njiru imangouma* (ichita nkhaba) *ngati manda..."* (Nyimbo Ya Solomo 8:6), mau amene Sauli anakwaniritsa pozunza Davide mzaka 20 zotsatirazo; Kumuthamangitsa Davide mozungulira ngati khoswe m'chipululu cha kum'mwera kwa dziko la Israeli.

Komalizira kwake Davide anakhala mfumu ya mfuko la Israeli, ndipo anawonetsa chikondi chake chachikulu kwa Mulungu pofuna kumanga nyumba yopemphereramo, kukumbukira zonse momwe Yehova anamuthandizira m'moyo wake pamene anali m'chipululu kuthawa ukali wa mfumu Sauli. Mulungu anamuyankha kuti mwana wa Davide, Solomo, ndiamene adzamange Nyumba ya mapemphero'yo ndinso kuti Mulungu anafuna kumumangira Davide nyumba (ufumu [2 Samueli 7:4-13]).

Kenaka Mulungu Yehova, anawonjezanso kulonjeza momveka bwino pobwereza zomwe analonjeza kwa Abrahamu ndipo mophatikizapo malonjezo ena popitiriza nkhani'yi:

"...Pamene masiku ako akadzakwaniridwa, ndipo iwe udzagona ndi makolo ako (Abrahamu), Ine ndidzaukitsa mbeu yako pambuyo

pako, imene idzaturuka m'matumbo mwako, ndipo ndidzakhazikitsa chimpando cha ufumu wake kunthawi zonse. Ndidzakhala atate wake, iye nadzakhala mwana wanga; akachita choyipa ndidzamalunga ndi ndodo ya anthu, ndi mikwapulo ya ana a anthu; koma chifundo changa sichidzam'chokera iye, monga ndinachichotsa Sauli amene ndinamuchotsa pamaso pako. Ndipo nyumba yako ndi ufumu wako zidzakhazikikadi ku nthawi zonse pamaso pako; mpando wa chifumu wako udzakhazikika ku nthawi zonse..." (2 Samueli 7:12-16).

Tikaona maphunziro angapo tawerenga aja, tiyembekezera kuti "mbeu" yonenedwayi ndi Yesu. Mafotokozedwe a Iye ngati mwana wa Mulungu (2 Samueli 7:14) atitsimikizira ichi monga momwemonso ndime zina m'Baibulo zikuchitira:-

- *"...Ine ndine ...muzu ndi mbadwa ya Davide, monga mwa thupi..."* (Aroma 1:3).
- *"...wochokera mu mbeu yake (Davide) Mulungu, monga mwamalonjezano anawautsira a Israeli mpulumutsi, Yesu;.."* (Machitidwe 13:23).
- Mngelo anamuwuzza Mariya m'dzakazi'yo za mwana wake, Yesu: *"...Iye adzakhala wamkulu, nadzatchedwa Mwana Wa Mkulukulu; ndipo Ambuye Mulungu adzampatsa Iye mpando wa Chifumu wa Davide atate (makolo) wake: ndipo Iye adzachita ufumu pa banja la Yakobo ku nthawi zonse; ndipo ufumu wake sudzatha..."* (Luka 1:32-33). Izi zikubvomerezanso pa malonjezano a mbeu ya Davide mu 2 Samueli 7:13 omwe akugwera ndinso kuyima mwa Yesu.

Monga mbeu ikudziwika mwa Yesu, zinthu zingapo tsopano zafukulidwa ndi zizindikiro zimenezi:-

-1) **MBEU**

"Mbeu yako...imene idzaturuka m'matumbo mwako... Ndidzakhala atate wake, iye nadzakhala mwana wanga;" *"...wa iwo okhala zipatso za thupi lako ndidzayika pamando wa chifumu wako"* (2 Samueli 7:12,14; Masalmo 132:10,11). Yesu, mbeuyo, idayenera kukhala mwana weni weni wa

Davide, ngakhale kuti bambo wake weni weni anali Mulungu. Izi zonse zikanatheka pokha pokha mwana'yo atabadwa mwa m'dzakazi ngati momwe Chipangano Chatsopano chikunenera; Mayi wake wa Yesu, Mariya, mwana wa Davide (Luka 1:32), koma analibe bambo wake weni weni wa padziko lapansi. Ichi chinali chinthu chozizwitsa chochokera kwa Mulungu kuti chiberekero cha Mariya chibale mwana mwa Mzimu Woyera natchedwa "Yesu", koteru, Mngeloyo anafotokozera motere:- **"...Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi ...choyeracho chikadzabadwa, chidzatchedwa Mwana Wa Mulungu..."** (Luka 1:35). Kubadwa "mwa M'dzakazi" kukutitsimikizira zonedwa m'malonjezano aja ndi maulosi ena omwe anapangidwa kwa Davide nakwaniritsidwadi mwa Yesu Khristu.

-2) NYUMBA YA MULUNGU

"...Iye adzamangira dzina langa nyumba..." (2 Samueli 7:13) zikuwonekeratu kuti Yesu ndi amene adzamange Nyumba ya Mulungu (yopemphereramo) m'masomphenya komanso m'chiphiphiritso cha nyumba ya uzimu. Ezekieli 40-48, akukamba za momwe nyumbayo idzamangidwire mzaka 1,000 zoyamba mu Ufumu Wa Mulungu (mzaka 1,000 zoyambirira mu Ufumu Wa Mulungu, Yesu akadzabweranso padziko lapansi lino), ndipo kuti nyumba'yo idzamangidwa ndi Iye mu Mzinda wa Yerusalemu. "Nyumba ya" Mulungu ndi yomwe Mulungu afunitsitsa kudzakhalamo mwaichi, Yesaya 66:1,2 akutifotokozera kuti Yehova adzabwera kudzakhazikika m'mitima mwa anthu omvera Mau ake. Yesu moteronso pakali pano, akumanga nyumba ya chipembedzo m'mitima mwathu kuti Mulungu azikhalamo, nyumba'yi ikumangidwa ndi zida (anthu) zomwe ndiwo okhulupirira onse m'choonadi omwense, tsopano anakhala ana a Mulungu. Titsimikizidwa zimenezi chifukwa Yesu anatchedwa Mutu wa Miyala ya pangodya yosankhidwa ndi Mulungu (1 Petro 2:4-8); ndipo a khristu ena onse akutchedwanso miyala yomangira nyumbayo yomwe ndi yoikidwa m'malo osiyana siyana a nyumbayo (1 Petro 2:5).

-3) MPANDO WA CHIFUMU

"...ndipo ndidzakhazikitsa chimpando cha Ufumu wake (wa Khristu) ku nthawi zonse...; Ndipo Nyumba yako ndi ufumu wako (wa Davide) zidzakhazikikadi ku nthawi zonse,"(2 Samueli 7:13,16 cp. Yesaya 9:6,7). Ufumu wa Khristu mwaichi, udzakhazikika m'ndondomeko ya Ufumu wa

Davide wa Israeli; Izi zikuonetsanso kuti Ufumu wa Mulungu’wu ndiko kupitirizidwa kwa Ufumu wa Israeli omwe udalipo kalelo ndikuti udzakhazikitsidwanso pansi pano – onani Phunziro 5.3 kuti muwerenge zambiri za nkhani imene’yi. Pofuna kukwaniritsa zonsezi, Khristu adzayenera kulamulira pa *“chimpando cha bambo wake Davide”* kapena malo omwe kunali ufumu wa Davide monga tawerenga m’Baibulo. Uku ndi ku Yerusalemu. Kotero, ichi ndi chitsimikizo chokwanira kuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwadi pansi pano pofuna ku kwaniritsa malonjezano amene’wa.

-4) UFUMU

“...Ndipo nyumba yako ndi ufumu wako (zonse) zidzakhazikikadi ku nthawi zonse pamaso pako” (2 Samueli 7:16); ndime iyi ikuonetseratu kuti Davide anayenera kuona Khristu akukhazikitsa Ufumu wa muyaya wa Mulungu. Choncho, awa anali malonjezano oyenera kuchitika kutsogolo kwa umoyo wa Davide kuti ndithu, iye, adzawukitsidwa ndipo adzadzionera yekha, pamene Khristu adzabweranso kudzakhazikitsa Ufumu wa Mulungu padziko lonse lapansi. Kotero, Khristu’yo (Mwana wake wa Davide), adzalamulira kuchokera mu Mzinda wa Yerusalemu.****

Zonsezi, zomwe zinalonjezedwa kwa Davide, ndi zinthu zofunikira kuzimvetsetsa kwambiri pa chiyembekezo chathu cha uzimu. Davide atazindikira kufunikira kwake kwa izi, ananena kuti ndi *“...pangano losatha,...Pakuti ichi ndi chipulumutso changa chonse, ndi kufuna kwanga konse”* (2 Samueli 23:5). Izinsu zikugwirizana ndi chipulumutso chathu; kusangalala komanso kukondwera pa izi chiyenera chikhale kulaka laka ndi kufuna kwathu nthawi zonse. Tiyenera tizindikirenso kuti chiphunzitso chotere ndi chofunikira kwambiri. Ndichinthu choopsa komanso chomvetsa chisoni kuwona kuti a khristu a matcharitchi ena amalimbikira kuphunzitsa zinthu zosiyana kwambiri ndi chiphunzitso cheni cheni choonadi monga chimenechi:-

- Ngati Yesu analipo kale asanabadwe, mwachitsanzo, kuti anali moyo, namayenda asanabadwe nawuka padziko lapansi, ndiye kuti zonse zomwe tawerengazi ziri chabe, malonjezano a kubadwa kwa Yesu kuti ndiye “mbeu” ya Davide kapena kuti mwana wa Davide, zinalibe tanthawuzo.

- Ngati Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwe Kumwamba, ndiye kuti Yesu sadzakhazikitsanso Ufumu wa Davide womwenso ndi wa ana a Israeli; komanso zingatanthawuzenso kuti Iye sadzalamulira pa chimpando cha Ufumu wa Davide kapena ku malo komwe Davide analamulirako. Ife tikudziwa kuti Yesu kapena mwana wa Davide wina aliyense sanalamulirepo dziko lapansi ngakhale tikuwerenga m’Baibulo kuti mbeu ya Davide, iyenera idzalamulire dziko lapansi; ndipo tawona kuti, “mbeuyo” ndiye Yesu. Koteru, tiyembekezerabe kuti Yesu akhazikitse Ufumu wa Mulungu padziko lapansi monga tawerenga m’Baibulo osati monga anthu amenenera.

KUKWANIRITSIDWA KWA ULOSI MWA MWANA WA DAVIDE , SOLOMONI

Mwana weni weni wa Davide, Solomoni, anakwaniritsa mbali ina ya malonjezano a Mulungu kwa Davide. Solomoni anamanga nyumba ya Mulungu yopemphereramo (1 Mafumu 5-8), ndipo adali ndi ufumu opambana ndi chitukuko cha mwana alirenji mu ulamuliro wake. Mayiko onse ozungulira Israeli ndi ena onse a kutali, ankatumiza nthumwi zawo pofuna kukapereka ulemu kwa mfumu Solomoni (1 Mafumu 10), ndipo anthu’wo ankadalitsika kwakulu mu uzimu akangolowa m’nyumba ya Mulungu ija yomwe anamanga ndi Solomoni. Tikhoza kunena kuti Solomoni anakwaniritsako zina mwa malonjezano a Mulungu kwa Davide choncho, sanakwaniritse zonse chifukwa sanalamulire dziko lonse lapansi komanso, Davide sanaonerere kukhazikitsa kwa Ufumu wake. Apa, tiona kuti ngakhale Solomoni, analosera za Ufumu weni weni wa Mulungu ulinkudzawo, wolamulidwa ndi Yesu Khristu monga tikuwerenga pa 2 Samueli 7 m’mwambamu.

Ena ananenapo kuti malonjezano kwa Davide anakwaniritsidwa mwa Solomoni; koma izi sizingagwirizane ndi zomwe tikuwerenga m’Baibulo:-

- Ndime zochuluka za m’Chipangano Chatsopano, chikuonetsa kuti “mbeu” ija siinali Solomoni ayi koma Yesu Khristu.
- Davide, akuwoneka kuti adalumikiza nkhani ya malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu ndi omwe iye analandira pamaso pa Mulungu (1 Mbiri 17:27 = Genesis 22:17,18).

- Ufumu wa Mulungu wokhazikidwa ndi “Mbeu” ija udayenera kukhalapo ku *“nthawi zonse”* kutanthauza kuti Ufumu’wo udayenera kukhala wa muyaya – Koma ufumu wa Solomoni siunali wamuyaya-unaatha!
- Davide anazindikira kuti malonjezano a Mulungu’wa ankakhudza komanso kugwirizana ndi chikonzero cha moyo wosatha omwe unakhudzanso onse a banja lake: *“...zoonadi nyumba yanga siikhala yotere ndi Mulungu; Koma Iye anapangana ndi ine pangano losatha;”* (2 Samueli 23:5).
- Mbeu ya Davide ndi Mesiya, Mpulumutsi Wathu ku machimo (Yesaya 9:6,7; 22:22; Yereimiya 33:5,6,15; Yohane 7:42). Koma onaninso kuti Solomoni sanamvere Mulungu nthawi yomaliza mu umoyo wake (1 Mafumu 11:1-13; Nehemiya 13:26) chifukwa adakwatira azimay ambiri a kumayiko a kunja kwa dziko la Israeli, chomwe chinali chinthu chosayenera pa chikonzero cha chiyembekezo cha chikhristu.

***MPATUKO 9: KUONONGEDWA KWA DZIKO
LAPANSI NDI KUMWAMBA (Chibvumbulutso 21:1;
2 Petro 3:6-12)***

Cholinga cha Mulungu ndi chikuti akhazikitse Ufumu Wake padziko lino lapansi (onani Phunziro 5), ndi zoonekeratu kuti Mulungu sangaliononge dziko lapansi n’cholinga chimene’chi; ndipo tawona kuti sicholinga Chake kutero monga taphunzira kale m’Phunziro 3.3 m’malonjezano Ake kuti sadzatero. Ndime ziri m’mwambazi zomwe zikukamba za kuwonongedwa kwa dziko koteru, ndichiphiphiritso chabe cha kueonongedwa kwa dziko (chikhalidwe) cha tchimo.

Mau a Petro, akuwonetsanso zifani fani pakati pa chiweruzo padziko lapansi nthawi ya Nowa mogwirizana ndi zomwe zidzachitike pa “tsiku lomwe Ambuye Yesu adzabwere mtsogolomo” *“...dziko lapansi la masiku aja, pomizika ndi madzi, lidaonongeka; koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mau omwewo zayikika kumoto, zosunga kufikira tsiku la chiweruzo ndi chiwonongeko cha anthu osapembedza...”* (2 Petro 3:6,7).

Petro akusiyanyitsa pakati pa chiwonongeko cha munthu ndi madzi m'nthawi ya Nowa mosiyana ndi chiwonongeko cha anthu pogwiritsa ntchito moto Yesu akadzabweranso. Tiwone kuti “dziko lakumwamba ndi lapansi” m'nthawi ya Nowa sizinawonongedwe – “zamoyo zonse” ndi zomwe zinawonongedwa (Genesis 7:21 cp. 6:5,12). “Kumwamba ndi dziko lapansi” kotero, zikuyimira zinthu zopangidwa ndi munthu padziko lino. Ena amene samamvetsa bwino ndime imeneyi, amayi wala kuti pakambidwa za kuwonongeka kwa kumwamba. Kumwamba sikungawonongeke chifukwa ndi kumene Mulungu amakhalako (Masalmo 123:11), ndipo kulibe tchimo lina lililonse (A Hebra 1:13; Masalmo 65:4-5), komanso kunabvomerezeka kuti Mulungu azikhala mu ulemberero (Masalmo 19:1). Mwaichi, ngati kumwamba kukambidwa mwanjira iyi, ndiye kuti ndi chiphiphiritso chomwe chikutanthawuza zinthu zina kuti ziwoneka motero, chimodzi modzinso mau ena angagwiritsidwe ntchito posimba za dziko lapansi.

Ndime zotsatirazi ndi zina mwa ndime zimene zikuwonetsa chiphiphiritso cha mtundu womwewu:-

- Mose nthawi ina anawauza ana a Israeli: **“...kumwamba kutchere khutu, ndipo ndidzanena; Ndi dziko lapansi limve mau a mkamwa mwanga;”**(Deuteronomo 32:1). Apa zikutitsimikizira motsindika kuti Mose anakalankhula kwa anthu a magulu awiri. Zikuwoneka kuti panali magulu awiri a anthu omwe adalankhulidwa ndi Mose.

1) **“Akulu onse a mafuko anu ndi akapitawo anu** ndinso

2) **“msonkhano wonse wa Isareli”** (Deuteronomo 31:28-30).

Akulu ndi akapitawo onse akuyimira **“kumwamba mwamba”** ndipo anthu wamba onse akuyimira **“dziko lapansi”**.

- Yesaya anayamba uneneri wake mochititsa chidwi: **“...Imvani miyamba inu (kumwamba), tchera makutu iwe dziko lapansi chifukwa Yehova wanena ...Imvani mau a Yehova inu olamulira...tcherani makuti kuchilamulo cha Mulungu wathu...”** (Yesaya 1:2,10). Tiwerenganso pano kuti pali kufanana pakati pa Kumwamba ndi atsogoleri; komanso pakati pa anthu wamba ndi dziko

lapansi. Utsogoleri (ulamuliro) uliwonse umachokera kumwamba kwa Mulungu polamulira anthu pa dziko lapansi.

- **“...Kumwamba adzayitana zakumwamba, Ndi dziko lapansi kuti aweruze anthu ake”**, anthu a mfuko la Israeli (Masalmo 50:4). Apa tadzimvera tokha.
- **“...Ndipo ndidzagwedeza amitundu (m'mayiko) onse ... (momwemonso) ndidzagwedeza miyamba (Kumwamba) ndi dziko lapansi”** (Hagai 2:7,21).
- **“...Pakuti lupanga langa lakhuta Kumwamba; taonani, lidzatsikira pa Edoma, ndi pa anthu amene ndawatemberera, kuti aweruzidwe...Lupanga la Yehova lakhuta ndi mwazi, lanona ndi mafuta ndi mwazi wa ana a nkhosa, ndi mbuzi, ndi mafuta a ipso ya nkhosa za mphongo; pakuti Yehova ali ndi nsembe m'Bozira, ndi ophedwa ambiri a m'dziko la Edoma”** (Yesaya 34:5,6). “Kumwamba” panonso kwalembedwa poyimira ndi kutanthawuza dziko la Edomu (lapansi); uneneri oyambirira kuti **“...Ndipo makamamu onse kumwamba adzasungunuka,”** (Yesaya 34:4) kotero, ayimira kusungunuka kwa dziko la Edomu; kutanthawuza kuti dziko la Edomu lidzafika potheratu ngakhale nthawi imene'yi lidali la mphamvu ndi la chitukuko.
- Kumwamba ndi dziko lapansi kuti zidasungunuka pa Yesaya 13, zitanthawuza kusungunuka kwa anthu a ku Babulo. Monga timawerenga za Babulo kuti **“...lidzagwedezeka kuchokera m'malo ake, m'kwiyo wa Yehova wa makamamu, tsiku la mkwiyo wake waukali. Ndipo padzakhala kuti monga mbawala yothamangitsidwa, ndi monga nkhosa zosazisonkhanitsa anthu, adzatembenukira yense kwa anthu ake nathawira yense kwa dziko lake”** (Yesaya 13:13,14). Kuthawa kwa kumwamba ndi dziko lapansi pano kwafanizidwa ndi kuthawa kwa anthu kuja. A Hebri 9:26 akukamba za “kutha kwa dziko” kuti zidayenera kuchitika m'chirumika choyamba Yesu atafa ndi kuukanso – kotero, kunali kutha kwa dziko la A Yuda.

Mogwiritsa ntchito mfundo imeneyi, tiwona kuti m' Chipangano Chatsopano tikawerenga za **“Kumwamba kwatsopano ndi dziko**

latsopano” pamene Khristu adzabweranso padziko lino lapansi, ndiye kuti akunena za chilongosoko chatsopano ndi Yesu pamene adzakhazikitse Ufumu wa Mulungu padziko lapansi.

- Tikawonetsetsa mofatsa pa 2 Petro 3, tidzatsimikizidwa za izi. Monga tafotokoza za kutha kwa dziko la “kumwamba ndi lapansi” mu ndime (chapter) 13 pamwambapa, tsopano tipitirire kuti “...*kotero ife monga mwa lonjezano, tiyembekezera kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano kumene kudzakhala chiyero ndi chilungamo...*” Apa tikumbukiranso za malonjezano a Mulungu pa Yesaya 65:17: “...*Pakuti taonani, ndilenga kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano;*” Tikawerenganso ndime zinazo pa Yesaya 65, tiona kuti zikutifotokozeranso utsopano wa Kumwamba ndi panso kuti pazonse, udzakhala wabwino, wangwiro ndi wopanda banga padziko lapansi lino.

“...taonani, ndilenga Yerusalemu wosangalala,...ndipo iwo sadzamanga nyumba wina nadzakhalamo; ...mwana adzafa wa zaka zana limodzi (mwachitsanzo, umoyo wa anthu udzatalika kotero, amene adzafa ali ndi zaka zana limodzi adzayesedwa ngati mwana) ...m’mbulu ndi mwana wa nkhosa zidzadyera pamodzi...” (Yesaya 65:18-25).

Madalitso a mtundu wotere adzachitika pamaso pathu mu Ufumu wa Mulungu, omwe udzakhazikitsidwe panso pano ndipo kudzakhala “Kumwamba kwatsopano ndi panso patsopano” zomwe zidzachotse mazunzo, mabodza ndi maboma onyenga anthu amene alipo pano’wa.

MPATUKO 10: ANTHU A KU BRITAIN AMANENA KUTI NDI ANA A ISRAELI

Pali anthu angapo monga bambo H.W. Armstrong omwe amanena kuti anthu a ku Britian ndi ana a Efraimu wa mfuko la Israeli, ndipo kuti anthu a ku America ndi ochokera mfuko la Manase wa Israeli. Iwo amanena izi m’bungwe lawo ndinso mkabuku kena komwe analemba kotchedwa “ Plain Truth” ndamanena kuti, malonjezano omwe anapangidwa kwa Abrahamu,

adakwaniritsidwa pakati pa anthu a ku America ndi Britain. Mamembala a bungwe lotchedwa “British Israelites” limakhulupirira kuti mafumu ndi mafumakazi a ku England, anabadwa kuchokera m’banja la Yuda lomwe lidayamba kudzera mwa mfumu Davide. Pofuna kukwaniritsa nkambakamwa zawo, amati a Yuda’wo, anakanidwa ndi Mulungu kotero, anasankha anthu a ku Britain m’ malo mwawo.

Tikaganizira zomwe taphunzira m’Phunziro 3, tiwoneratu kuti izi sizoonna ayi. Tiwonjezere taphunzira kalezo ndi mfundo zotsatira’zi:-

- Anthu onse ndi ochimwa pa chibadidwe (Aroma3:23), ndipo kuti Khristu anafa kuti anthu onse padziko lapansi akhale nawo mwayi opulumutsidwa mwa Yesu Khristu’yo. Izi sizikukhudza dziko lina lirilonse kapena mtundu wina uliwonse ayi; Koma kuti tiyenera kubatizidwa mwa Yesu m’choonadi kuti tikhale ana a Israeli a uzimu m’chipembedzo (Agalatiya 3:27-29). Tinawuzidwa kuti udindo wathu ndi kulalikira Uthenga Wabwino ku mayiko onse, kuwabatiza onse okhulupirira payekha mwa Khristu (Marko 16:15,16); Ndipo mwaichi, Israeli watsopano apangidwa ndi anthu a m’mayiko onse osati a ku Britain okha monga iwo akunenera ayi.
- Monga tawerenga, kungakhale kobvuta kwambiri kuti tipeze ngati ndi zoonna kuti anthu a ku Britain ndi America kuti anachokera m’ mabanja a chi Yuda. Onse ndi anthu ochokera m’mayiko osiyana siyana m’dziko lapansi. Chon’cho, munthu akangobadwira m’dziko la Britain kapena America sindiye kuti ndi osankhidwa ndi Mulungu, kapena kuti ndi anthu opatulika ayi.
- A bungwe la “British Israelites” amanena kuti malonjezano a mwana wa Abrahamu anakwaniritsidwa mwa iwo ngakhale iwo sanamvere Mulungu, kotero sikunali koyenera iwo kuti asunge malamulo. Chachikulu kwa iwo chinali kubadwa m’dziko la Britain! Izi ndi zoonkeratu kuti zikutsutsana ndi cholinga cha Mulungu chomwe chiyenera kukwaniritsidwa pomvera malamulo ake. Levitiko 26 ndi Deuteronomo 28, tiwerengamo za madalitso omwe angabwere ku mfuko la Israeli ngati amvera Mau Ake, komanso za matemberero omwe angabwere chifukwa cha kusamvera. Mwaichi, kunena kuti anthu a ku Britain analandira madalitso chifukwa chakuti ndi nzika za

dziko la Britain, n’kutsutsana kwambiri ndi ndondomeko ya chipulumutso yomwe Mulungu anakonza. Mulungu sangapereke madalitso kwa anthu osamvera ayi.

- Kunena kuti Mulungu anawataya anthu ake a ku Israeli ndipo m’ malo mwake anasankha anthu a ku Britain, n’kukana choonadi cheni cheni monga timawerenga pa Aroma 11:12; **“...Mulungu anataya anthu ake kodi? Msatero ai. Pakuti inenso (Paulo) ndiri M’Israeli, wa mbeu ya Abrahamu wa mfuko la Benjamin. Mulungu sanataya anthu ake amene Iye anawadziwiratu...”**
- Ufumu wa Mulungu udali Ufumu wa ana a Israeli kalelo (2 Mbiri 9:8). Ufumu’wu unaphwanyidwa chifukwa chakusamvera kwa ana a Israeli, koma udzakhazikitsidwanso (Ezekieli 21:25-27). Komanso ufumu’wo udzakhazikidwa ndithu ndipo likulu lake lidzakhala Yerusalemu (Mika 4:8) ndikuti Yesu ndi amene adzalamulire pa chimpando cha mfumu Davide (Luka 1:32).
- Ana a Israeli omwe anamwazika m’ malo osiyana siyana m’ dziko lonse lapansi, adzakusidwa nasonkhanitsidwa pamodzi ku Yerusalemu: **“...ndidzatenga ana a Israeli pakati pa a mitundu kumene adamkako, ndi kuwasokolotsa kumbali zonse, ndi kulowa nawo m’ dziko mwao; ndipo ndidzawayesa mtundu umodzi m’ dzikomo, pa mapiri a Israeli; ndipo mfumu imodzi idzakhala mfumu ya iwo onse...”** (Ezekieli 37:21,22). Izi zikukwaniritsidwa lero pamene tikuona a Yuda onse omwe adamwazikana nakakhazikika m’ mayiko osiyana siyana, tikuwaona akubweranso kukakhala m’ misasa yawo yomwe inamangidwa ndi boma la Israeli. Ndipo tikudziwa kuti ichi n’chikonzero cha Mulungu, kuti kusonkhana kweni kweni kudzakwaniritsidwa pamene ana a Israeli wa chiyero adzasonkhanitsidwe zeni zeni mu Ufumu Wa Mulungu ulin’ kudza’wo.

Onse omwe angasangalatsidwe kuwerenga mozama pa zomwe mwaphunzira panopa’zi mukhoza kuyitanitsa timabuku tofotokoza mwachindunji nkhani’yi ku ma adiresi apatsidwa komalizira kwa buku lino.

PHUNZIRO 3: MAFUNSO

1. Ndimalonjezano ati omwe akuwonetsa kuti pangakhale kulimabana kwamphamvu pakati pa tchimo ndi chiyero?
 - (a) Lonjezo kwa Nowa
 - (b) Lonjezo la m'munda wa Edeni
 - (c) Lonjezo kwa Davide
 - (d) Lonjezo kwa Isake
 - (e) Lonjezo kwa Abrahamu
2. Ndi malonjezano ati omwe ali owona pokamba zochitika m'malonjezano a m'munda wa Edeni?
 - (a) Mbeu ya njoka ndi Lusifala (Satana)
 - (b) Khristu ndi onse oyera mtima ndiwo mbeu ya mkazi'yo
 - (c) Mbeu ya njoka inabvulazidwa mongoyembekezera ndi Khristu
 - (d) Mbeu ya mkazi inabvulazidwa ndi imfa ya Khristu
 - (e) Mbeu ya njoka inabvulazidwa kwathunthu ndi Khristu
3. Ndi kuti kumene mbeu ya Abrahamu idzakhazikikeko mpaka muyaya?
 - (a) Kumwamba
 - (b) Mu Mzinda wa Yerusalemu
 - (c) Padziko lapansi lino
 - (d) Ena Kumwamba ndi ena Pansi pano.
 - (e) Mlengalenga
4. Ndi malonjezano ati mwa otsatira'wa omwe anapangidwa kwa Davide?
 - (a) Kuti mwana wake woyamba adzalamulira mpaka muyaya
 - (b) Kuti mbeu yake idzalandira Ufumu Kumwamba
 - (c) Kuti mbeu'yo idzakhala Mwana Wa Mulungu
 - (d) Kuti mbeu yake, Yesu, adzakhala kumwamba asanabadwe pansi pano
 - (e) Kuti Ufumu Wake udzakhlapo mpaka muyaya
5. Kodi ife tingakhale nawo bwanji "Mbeu" ya Abrahamu?
6. Kodi dziko lapansi lidzaonongedwa?
7. Kodi malonjezano a Mulungu akutsimikizira bwanji pa yankho lanu mu mfunso nambala 6 m'mwambamu?
8. Fotokozani mwachidule za malonjezano a m'munda wa Edeni pa Genesis 3:15.

Mukayankha chonde tumizani mayankho anu ku imodzi mwa ma adiresi alembedwa komali kwa buku lino:

PHUNZIRO 4

MULUNGU NDI IMFA

4.1 UTHUNTHU WA MUNTHU

Anthu ambiri lerolino samatha kuganizira za imfa komanso chilengedwe cha uthunthu wao chomwensho ndi chiyambi cha imfa. Chifukwa chosazindikira zinthu zimenezi, anthu amatha kukhala umoyo wao onse osadziwa zoonza zeni zeni za iwo okha ndipo mwaichi, saatha kuona za kufunika kodziwa gawo limeneri kwathunthu; Koteru, amaangochita zonse molankhulidwa ndi zofuna ngakhale zilako lako za thupi lawo. Munthu lero samalola kuti umoyo uno ndi ongoyembekezera ndipo kuti ndithu umoyo wathu ndi waufupi chifukwa chakuti tsiku lina lirilonse tikhiza kufa monga momwe anzathu ena anafera. *“...Moyo wanu uliwotani? Pakuti muli utsi, wakuoneka kanthawi, ndi pamene ukanganuka...”* *“Pakuti kufa tidzafa, ndipo tiri ngati madzi otayika panso amene sakhoza kuwaolanso; “...akhala ngati msipu wophuka. Mamawa uphuka bwino (ubwino wathu) Madzulo ausenga, nuuma...”* (Yakobo 4:14); 2 Samueli 14:14; Masalmo 90:5,6). Mose ngati munthu ozindikira, anapepa kwa Mulungu: *“...Mutiphunzitse kuwerenga masiku a moyo wathu motero, kuti tikhale nawo mtima wanzeru...”* (Masalmo 90:12). Choncho, mwaichi, tikhale ndi chithunzi thunzi chakuona ubwino wodziwa zambiri za moyo wathu, kufunika kokhala ndi nzeru za uzimu m’choonadi ndipo kuti izi zikhale zoyambirira kuchita nthawi zonse.

Anthu timasiyana kwambiri m’kazindikiridwe ka zotsatira za imfa mu umoyo wa munthu wakufayo. Anthu enanso, anangozowera ngati kuti imfa ndi mbali imodzi ya moyo wao wa tsiku ndi tsiku koteru, sakhalanso ndi chidwi china chirichonse pa zotsatira za imfa’yo kwa munthu wakufa. Akhristu ambiri amakhulupirira kuti mkati mwamunthu muli “kamzimu kosafa”; komwe ngakhale munthuyo akafa, kamzimuko kamauluka kuchoka mthupi’lo nkupita kumwamba komwe kamakalandira mphotho ya moyo kapena chilango chosatha. Tiyeni tizindikire pano kuti mfundo zoterezi zidapangidwa ndi munthu chifukwa chakuti munthu’yo saamafuna kudziwa bwino zomwe Baibulo limanena za imfa, ndinso kuti uthunthu wa munthu m’Baibulo udafotokozedwa bwanji. Mutu umenewu ndi obvuta kuwumvetsa mwaife tokha maka maka ngati sitingaganizire zomwe malembo a m’Baibulo amafotokoza pamene tafuna kutsutsa kapena kubvomereza nkhani zabodza komanso zoonza, ngati m’mene

tikuchitira posinkha sinkha zimenezi m’buku lino. Tisayiwale kuti bodza linayamba m’unda wa Edeni ndi njoka yochenjera ija. Mosiyana kwambiri ndi zomwe timawerenga m’Baibulo kuti **“udzafa ndithu”** ngati tichimwa (Genesis 2:17), njoka ija inamunamiza munthuyo kuti **“kufa simudzafayi”** (Genesis 3:4). Kuchokera pamene, bodza lazanga mitima ya anthu lero pokhudza tanthawuzo leni leni la imfa ndi chimene chimachitika munthu akafa. Zipembedzo zambiri zidabvumbulutsidwa chifukwa chosamvetsetsa, momwemo, zipembedzozo tsopano zikutsata mfundo zabodza pokhudza mamasulidwe a imfa kotero, mamasulidwe’wo akumasiyana koposa ndi Malembo Oyera. Mwachisoni, anthu omvera nawonso samatha kuona paokha chifukwa chosakhala ndi chidwi komanso alibe mwayi ozindikira zambiri pa Malembo Oyera okhudza nkhani ngati imeneyi. Chosangalatsa chachikulu apa ndi chakuti pamene timawerenga m’Baibulo za imfa, zimatipatsa chithunzi choyenera nthawi zonse monganso kunalembedwa pa 1 Akorinto 15:13-17. Paulo akukamba zambiri zoonza zokha zokha pa nkhani zosiyana siyana pa chipulumutso chathu m’ndime imeneyi.

Kuti timvetse bwino za uthunthu wa munthu, tiyeni tiganizirenso za chilengedwe cha munthu chomwe timawerenga m’Baibulo. Mau amenewa amawonetseratu momwe thunthu la munthu lili posachotsera kapena kuwonjezerapo mau ndi maganizo athu omwe angatsutsane ndi zimene zinalembedwa m’Baibulo (onani Mpatuko 18 pofuna kuzindikira zeni zeni m’Buku la Genesis). **“Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wa moyo m’mphuno mwache;..ndiwe mpfumbi (Adamu) ndi kumpfumbiko udzabwerera”** (Genesis 2:7; 3:19). Tikawerenga ndime zimenezi zomwe zikufotokoza za chilengedwe cha munthu, tiona kuti sitinauzidwepo za “kamzimu kosafa” komwe kamapezeka mwa munthu wolengedwayo. Pali dothi ndi mpweya owuziridwa ndi Mulungu basi, kotero, munthuyo anayamba kupuma. Malo onse a ziwalo za munthu, zonse za munthu’yo akafa nazonso zimafa.

Baibulo likutitsimikizira kuti munthu thunthu lake lose ndi dothi: **“..ife tiri dongo”** (Yesaya 64:8); **“munthu woyambayo ali wapansi, nthaka,”** (1 Akorinto 15:47); Munthu **“maziko ake onse ali m’mpfumbi”** (Yobu 4:19); **“..Ndi munthu adzabwereranso ku mpfumbi”** (Yobu 34:14,15). Abrahamu naye, anabvomereza kuti iye analidi mpfumbi **“..ine ndine mpfumbi ndi phulusa”** (Genesis 18:27).

Munthu atangochimwa m'munda wa Edeni uja, nthawi yomweyo Mulungu anamuchotsa m'mundamo chifukwa sanamvere malamulo ake; *“..Ndipo anamuyingitsa munthuyo; (anamuthamangitsa m'mundamo)...Kuti asatambasule dzanja lake ndikutenga za mtengo wa moyo, ndikudya ndikukhalanso ndi moyo nthawi zonse”* (Genesis 3:24, 22). Tione kuti zikanakhala kuti munthu ali ndi kambali kena kamkati mwa thupi lake komwe sikamafa (mzimu), sizikanakhala zoyenera kuti Mulungu amuthamangitse m'munda wa Edeni uja. Mulungu pomuthamangitsa munthu m'munda muja, sanafune kuti munthu wochimwayo apezenso moyo wosatha mosazindikira udindo wake ndi kufunika kwake komvera Mulungu pongodyanso zipatso za mumtengo wa moyo'wo m'mundamo. Choncho, n'kofunikira kumvetsa kuti munthu akafa, palibe mbali ina ya thupi lake lomwe limakhalanso ndi moyo.

NJIRA YOMWE IFE TINGAPEZERE NAYO MOYO WOSATHA

Kawiri kawiri timamva za Uthenga Wabwino kuti munthu ali ndi mwayi wopeza moyo wosatha wa nthawi zonse zosatha, chifukwa cha ntchito yabwino ya Yesu Khristu. Iyi ndi njira yokhayo yopezeka m'Baibulo kuti munthu alandirensa moyo wosatha omwe unachotsedwa mwa iye ndi Mulungu m'munda wa Edeni muja. Baibulo silimakambapo kanthu kalikonse kuti munthu akafa, iye kapena mzimu wake umapita kumwamba. Mwaichi, palibenso za kubvutika kosatha kwina kulikonse komwe kumaoneka munthu akafa chifukwa cha machimo monga ena amanenera; Koma kuti ochimwa onse sadzakhala nawo mwayi odzaukitsidwa kumka kumoyo wosatha mu Ufumu Wa Mulungu Yesu akadzabweranso. Munthu akafa amabwerera ku dothi kumene anachokera monga tawerenga kale. Kotero, kuti munthuyo apezenso moyo wosatha m'chiyero pamaso pa Mulungu, ayenera kumvera malamulo a Mulungu ndipo adzalandira mphotho chifukwa cha chilungamo ndi kumvera kwakeko. Popanda chilungamo ndi chiyero mwa Yesu Khristu, munthu adzakhalabe dothi chiweruzo chikadzachitika patsiku lobwera Ambuye Yesu Khristu.

Ndime zotsatirazi zikutitsimikiziranso kuti kulandira moyo wosatha ife tiyenera tichitepo kanthu ndiponso kuti sitingawulandire mwachilengedwe chathu kapena m'chibadidwe chathu ayi. Kotero, tidziwadi kuti mwachilengedwe chathu, ife tidzabwerera ku nthaka ndikuti pokha pokhapo titachitapo kanthu:-

- **“..Khristu ..wabweretsa moyo, inde moyo wosatha, naonetsera poyera moyo ndi chosabvunda mwa Uthenga Wabwino...”** (2 Timoteo 1:10; 1 Yohane 1:2).
- **“...Ngati simukudya thupi la Mwana wa munthu ndi kumwa mwazi wake, mulibe moyo mwa inu nokha** (mwachitsanzo, wa chibadidwe). **Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wanga ali nawo moyo wosatha; ndipo ine ndidzamuwukitsa iye tsiku lomaliza...”** (Kumupatsa) **“moyo wosatha”** (Yohane 6:53,54). Yesu akutikumbutsa kuti ife timutenge ngati kuti **Iye “ndi mkate wamoyo”** ndipo kuti tikamulandira pomumvera Iye, tidzakhala nacho chiyembekezo cha moyo wosatha chimenechi (Yohane 6:47,50,51,57,58).
- **“Mulungu anatipatsa ife** (wokhulupirira) **moyo wosatha, ndipo moyo umenewu uli mwa Mwana wake”** (1 Yohane 5:11). Sipangakhale chiyembekezo china chirichonse cha moyo wosatha kwa ena onse omwe sakhulupirira kudzera **“...mwa Yesu Khristu”** chipulumutso m’moyo wosatha chimapezeka kudzera mwa Yesu yekha; Iye ndiye **“mkulu ndi mlembi wa moyo** (wosatha)” (Machitidwe 3:15) -Iye **ndiye “mkulu ndi wamphamvu wa chipulumutso kwa onse akumvera Iye”** (A Hebri 5:9). Moyo wosatha kwa munthu kotero, udzadza ndi chikhulupiriro mwa Khristu ndipo kuti mwayi wotere unadza chifukwa cha ntchito ya Khristu.
- Mkhristu weni weni wokhulupirira amafuna funa moyo wosatha momwemo, adzalandira mphotho iyi popatsidwa mphatso ya moyo wamuyaya omwe lero akadalibe (Aroma 1:7; 6:23; Yohane 10:28). Pakuti **“chobvunda ichi** (thupi lathu lakufa tiri naloli) **chiyenera kubvala chisabvundi, ndi chaimfa ichi kubvala chosafa”** pamene Khristu adzabweranso (1 Akorinto 15:53); Kotero, moyo wosatha ndi lonjezo lomwe Yehova Mulungu anapanga kuti udzalandiridwe ndi anthu okhawo okhulupirira osati lero koma panthawi irinkudzayo yomwe Mwini Mulungu anakonza (1 Yohane 2:25).

- Pakadali pano, ndi Mulungu Mwini Yekhayo amene ali ndi moyo wamuyaya wa chikhalire kuchokera pachiyambi (1 Timoteo 6:16).

4.2 THUNTHU - (MZIMU)

Monga taphunzira, tidziwa tsopano kuti munthu alibe kanthu kena kalikonse mkati mwa iye yekha kamene sikamafa. Tikatero, titha kuzindikira bwino tsopano mopanda kusokonekera powerenga liwu loti “mzimu”.

Mau amene amamasulidwa *“mzimu”* m’Chichewa, kuchokera mzilankhulidwe za chi Hebrai ndi chi Greek m’Baibulo, ndi *“Nephesh”* ndi *“Psuche”* ndipo m’ndime zotsatirazi mau’wa anamasulidwa motere:-

Thupi	Iye yekha
Thunthu	Mpweya
Chinthu	Mtima
Maganizo	Munthu

Mau amenewa kotero, ayenera kutanthauzidwa kuti *“munthu”*, *“thupi”* kapena thunthu lonse la munthu palokha. Mau a m’Chingerezi omwe mwachidule amalembedwa kuti S.O.S. (Pa Chizungu mau onse ndi “Save our Souls”) amatanthawuza kapena tinganene kuti “tipulumutseni ku imfa” m’Chichewa. Choncho, liwu limeneli, lomwe m’Baibulo la Chichewa limatanthawuzidwa kuti “Mzimu”; lidayenera kutanthawuzidwa kuti *“munthu, chinthu”* kapena *“inu”* monga zirili m’ndime zina m’Baibulo lathu’li. Ma Baibulo ambiri a masiku ano a m’Chingerezi, akutanthawuzidwa bwino pofuna kupereka matanthawuzo eni eni a Mau a Mulungu m’Baibulo limene lidalembedwa koyambirira. Chitsanzo chabwino pa nkhanu’yi ndi Baibulo la N.I.V. (The New International Version) lomwe limatanthawuzira kuti *“inu, munthu, thupi, iye yekha”* m’ malo momwe

Baibulo lakale lidatanhawuzira kuti *“Mzimu”*, “soul”. Nyama zomwe Mulungu analenga zimatchedwa *“zamoyo zoyenda”* (pachizungu “living creatures” kutanthawuza kuti *“zamoyo zoyenda yenda”* [Genesis 1:20,21] monganso *anthu* ali mgulu lomweli!; zomwe m’Chingerezi ndi *“Soul”* [soul] ndipo mau ake m’chi Hebri ndi m’chi Greek ndi amodzi omwewo otchedwa *“nephesh”* ndi *“psuche”* *“..Ndipo...munthuyo* (“nephesh, soul”) *nakhala ndi moyo* (“living creature”); monga nyama ziri zamoyo! Kusiyana komwe kulipo pakati pa nyama ndi munthu ndiko kwakuti, munthu anapatsidwa mwayi ndi Mulungu woti aziganiza kwambiri kuposa momwe nyama zimaganizira komanso kuti iye, anapatsidwanso udindo woyang’anira nyamazo. Iye (munthu) analengedwa m’maonekedwe, m’chifanizo, m’chikhalidwe, komanso m’chithunzi thunzi cha Mulungu (Genesis 1:26; onaninsu Phunziro 1.2). Ndipo anthu ena amayitanidwa kuti akadziwe Uthenga Wabwino omwe umawaunikira ku chiyembekezo cheni cheni cha moyo wosatha chomwe tsopano, chimatsegulidwa kwa iwo m’chiyero cha Mulungu (1 Timoteo 1:10). Apa tikaona, tizindikira tsopano kuti palibe kusiyana pakati pa ife anthu ndi nyama mu umoyo wathu ndi imfa yathu:-

“Pakuti chomwe chigwera ana a anthu chigweranso nyamazo; ngakhale chogwera n’chimodzi (onani kuti ife ndi nyama zimatigwera mofanana – imfa imene imagwera nyama ndi yomwensu imagwera ife anthu) *monga winayo angofa momwemo zinazo zifanso; inde onsewo ali ndi mpweya umodzi; ndipo munthu sapambana nyama pakuti zonse ndi chabe. Onse* (mwachitsanzo, nyama ndi munthu) *apita malo amodzi* (kumanda [m’dzenje], pansu pa nthaka); *Onse achokera ku mpfumbi ndi onse abwereranso ku mpfumbi,”*(Mlaliki 3:19,20). Mlembi wa Buku la Mlaliki adapemphera kwambiri kwa Mulungu kuti Uthenga umenewu umveke ndikutinso ukalandiridwe ndipo kotero, anthu akadziwedi ichi *“...kuti Mulungu awayese ndi kuti* (anthu) *akazindikire eni ake kuti iwo ndiwo nyama zakuthengo”* (Mlaliki 3:18). Chifukwa chaichi, tiwona kuti nkobvuta kuti anthu angalolere kulemekeza Uthenga wa Yehova wotere, popeza iwo eni samafuna kufanana ndi nyama monga Baibulo likunena kuti Mulungu Mwiniyo anakonza izi zikhale motero ndipo kuti Iye Mwini, amafuna ife tizindikire choonadi chimenechi mwa malembo ake Oyera. Choncho, n’chifukwa chake Mulungu ananeneratu kuti ndi anthu ochepa okhawo amene adzalandire chipulumutso, popeza ndi ochepadi amene amazindikira kuti iwo samasiyana ndi nyama pa chilengedwe cha Mulungu. Baibulo la

m'Chingerezi la N.I.V. linanthawuzira Mlaliki 3:18 kuti **Mulungu “amayesa” munthu** pomuzindikiritsa kuti iye adziwe kuti ali nyama wamba mwachitsanzo, okhawa amene angathe kudzichepetsa kukhala anthu ake okhulupirika pololera choonadi ngati chimenechi; Koma onse amene amakana choonadi chimenechi, namati akafa, mzimu wao umapita kumwamba, kufuna kudziyanitsa pakati pa iwo ndi nyama, amalephera muyeso umenewu wa Mulungu popeza Yehova sadasiyanitse pakati pa nyama ndi munthu. Munthu, wakhala akufalitsa maganizo ake a bodza pofuna kudzikweza iye yekha kotero kuti, adziwonetsere iye kuti ali wamphamvu kuposa chilengedwe china chirichonse. Nthawi zina ngakhale mitundu ina ya anthu, yakhala ikudzikweza n'cholinga chakuti iyo ikhale yopambana anzawo ena onse padziko lapansi, pomanena kuti iwo amakondedwa ndi Mulungu kuposa ena onsewo. Tinene pano kuti izi ndi zosiyana kwambiri ndi chiphunzitsa choonadi cha Baibulo lomwe ndiye Mau eni eni a Mulungu. Davide m'mau ake pa Masalmo 39:5 akuwonetsera kuti poyera komanso, tikhoza kuthandizika powerenganso mau ngati amenewa m'ndime iyi; **“munthu kwa iye yekha ali chabe,” “Sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ake”** (Yeremiya 10:23).

Chomwe tingadziwe za m'Baibulo ndi chakuti anthu onse, inde zamoyo zonse, komalizira kwake zimafa. Choteronso, mzimu (soul, nephesh, psuche etc), umafanso ndipo kuti zonse mwa munthu zimabwerera ku nthaka pamene mpweya wa munthu kapena nyama umabwerera kwa Mulungu yemwe ali Mwini wake (amene adawuzira). Timamva kuti mizimu (anthu [souls] eni eni) ambiri anafa, kotero, zimatitsimikiziranso kuti palibe mbali ina iriyonse ya gawo lina la munthu limene limakhalabe ndi moyo pamene munthuyo wafa. Onaninsu zambiri pamutu umenewu powerenga ndime zotsatirazi:-

- **“..moyo (soul, nephesh) wochimwawo ndiwo udzafa”** (please note Chichewa Bible translation errors [Ezekieli 18:4]).
- Mulungu atha kuwononga moyo ndi thupi lomwe ngakhale liri m'manda kapena likuyenda nthawi ina iriyonse (Mateyu 10:28). Pali ndime zinanso zimene zimakamba za kuwonongedwa kwa mzimu (soul) monga ndime zotsatirazi; (Ezekieli 22:27; Miyambo 6:32; Levitiko 23:30).

- Miyoyo yonse (m'Chingerezi – “all souls”) ya Mzinda wa Hazori inawonongedwa, inakanthidwa ndi lupanga lakuthwa (Yoswa 11:11;cp.10:30-39).
- “...*Chirichonse cha moyo* (all living souls including man) *chimafa*” (Chibvumbulutso 16:3; cp. Masalmo 78:50).
- Kawiri kawiri malamulo a Mose ankalamula kuti munthu (soul, nephesh) yemwe sadzamvera malamulo ena, ayenera kufa ndithu (Numeri 15:27-31).
- Ndime zambiri zimene zimakamba za mzimu (soul) kuti umakondwa kapena kupanikizidwa, umalira kapena kumva njala, ndi ndime zimene zimamveka bwino komanso kutsimikizira kuti mzimu ndi chinthu chimene chimapotedwa motere; mau amenewa angakhale ndi tanthawuzo mwaife pokha pokhapo titamvetsadi kuti munthu (mzimu) amafa, osati kumalalikira zabodza pofuna kufanana ndi zipembedzo zina zimene ziri ndi zikhulupiriro zosayenera, zomwe sizipezeka pena paliponse m’Baibulo ayi (Miyambo 18:7; 22:25; Yobu 7:15).
- “...*palibe amene adziwa kusunga moyo (soul) wake*” (Masalmo 22:29).
- Khristu “..*anathira moyo (soul) wake kuimfa* kotero “*mzimu*” kapena “*moyo*” wake unaperekedwa kuti ukhale nsembe ya tchimo (Yesaya 53:10,12).

Apa taonadi kuti “mzimu” ngati momwe liwuli lalembedwera m’Baibulo, limatanthawuza kuti ndi munthu, thunthu kapena thupi osati kanthu kena kamene sikamafa komanso kuti kamakhala mkati mwa thupi lathu ayi. Werengani zitsanzo zina zotsatirazi:-

- “..*mwazi wamiyoyo* (souls–mizimu) *yosachimwa ya umphawi* (Yeremiya 2:34).

- *“Ndipo munthu (soul) akachimwa, wakuti adamva Mau akuwalumbiritsa.. kapena osakamba kanthuko...kapena munthu (soul!) akakhudza chirichonse chodetsa...kapena munthu (soul) akalumbira, kulumbira ndi milomo yake”* Levitiko 5:1-4).
- *“...moyo (soul) wanga; Ndi zonse ziri mkati mwanga...lemekeza Yehova Mzimu wanga (soul!)...Amene akhutitsa mkamwa mwako ndi zabwino”* (Masalmo 103:1,2,5).
- *“Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wake (his soul!) adzautaya; ndipo yense wakufuna moyo wake (his soul) chifukwa cha Ine,adzaupulumutsa”* (Marko 8:35).

Ichi ndi chitsimikizo chokwanira kwaife kuti tiyenera tidziwe kuti mzimu (soul), siliwu limene limatanhawuza ngati kanthu kena kauzimu mkati mwa munthu, komwe kamakhala kachikhalire kosafa ayi; liwuli monga tafotokoza kale kuti m’chi Greek, limatanhawuza kuti ndi thupi komanso moyo wathu kotero, monga m’mene mau’wa analembedwera m’Baibulo, sakuyimira kanthu kena kalikonse komwe sikamafa ayi.

- Numeri 21:4 akuonetsa kuti gulu la anthu likhoza kukhalanso ndi *“mtima umodzi” (one soul)*. Mtima (mzimu) kotero, sukuyimira kanthu kena kalikonse kamoyo mkati mwathu ayi.

4.3 MZIMU WA (MPHAMVU YA) MUNTHU

N’zomvetsa chisoni kuti chifukwa chosafuna kumvetsetsa zimene Baibulo limanena pa Mau ena lero, pali chisokoneza chachikulu pakati pa anthu m’matanthawuzidwe a liwu loti “soul” ndi “spirit”. Izi zikuchitika chonchi popeza mau awiri’wa amamasuliridwa mofanana m’Chichewa komanso

mzilankhulidwe zina zambiri. Liwu loti “soul” (mzimu) monga tanena kale, limene limayimira magawo onse a munthu kuphatikizapo moyo wake (mpweya), litha kusokonezedwa m’matanthawuzo ake ndi liwu loti “spirit” (mphamvu). Tikawona momwe mau’wa amagwiritsidwira ntchito m’Baibulo, tiona kuti ndi osiyana m’matanthawuzo ake (A Heberi 4:12).

Mau oti “spirit” (mzimu kapena mphamvu) m’Chi Heberi ndi chi Greek, ndi “Ruach” ndinso “Pneuma” amene amatanthawuzidwanso m’Chichewa kuti:-

-Moyo	-Mzimu
-Maganizo	-Mphepo
-Mpweya	

Taphunzira kale za mzimu m’Phunziro 2.1 kuti Mulungu amagwiritsa ntchito Mzimu wake (Mphamvu zake) kuti cholinga cha chilengedwe chisungidwe pophatikizapo munthu. Mzimu wa Mulungu (Mphamvu ya Mulungu) umene uli mwa munthuyo kotero, ndi moyo (mpweya) mwa munthuyo. **“...Pakuti monga thupi lopanda mzimu (mpweya) liri lakufa...”** (Yakobo 2:26) **“Mulungu ...anauzira mpweya (mzimu) wa moyo m’mphuno mwake (mwa Adamu); ndipo munthuyo nakhala wamoyo (a living soul!) (Genesis 2:7).** Yobu akukambanso za “Mzimu Wa Mulungu kuti **“ndi mpweya” wake wa m’mphuno zake**” (Yobu 37:3 cp. Yesaya 2:22). Mzimu (mpweya) wa moyo mwa ife choncho, unapatsidwa kwaife pa nthawi yomwe tinkabadwa ndipo timakhala nawo mpaka tsiku lomwe yense waife amafa. Pamene Mzimu Wa Mulungu uchotsedwa mwa chinthu chirichonse, chinthucho chimafa nthawi yomweyo. Ngati Mulungu **“...Akadzisonkhanitsa yekha Mzimu (Mphamvu) wake ndi mpweya wake; Zamoyo zonse zidzatsirizika pamodzi, ndi munthu (soul) adzabwerera ku mpfumbi. Ngati tsono uli nako kuzindikira, tamvera ichi”** (Yobu 34:14-16). Tiyeneradi kuzindikira ndi kumvera zimenezi zomwe ndi zochokera m’Buku Lopatulika.

Pamene Mulungu achotsa mzimu wake (mphamvu yake) mwaife, tiyenera kufa, thupi lathu lonse limafanso; ndipo sitingathenso kukumbukira chifukwa zonse zafa mwaife. Kotero, Davide anazindikira kuti sayenera kukhulupirira munthu ayi koma kuyika chikhulupiriro chake pa Mulungu amene ali Mwini zonse.

Masalmo 146:3-5 akunena mosabisa potsimikizira nkhani imeneyi kuti zonena za munthu ndi zopanda tanthawuzo: “...*musamakhulupirira zinduna, kapena mwana wa munthu, amene mulibe chipulumutso mwa iye. Mpweya* (Mzimu) *wake uchoka, abwerera kumka ku nthaka yake* (kumene ife tinachokera); *Tsiku lomwelo zoganiza zake zitha. Wodala munthu amene akhala naye Mulungu wa Yakobo kuti am’thandize*”.

Panthawi ya imfa, “..*mpfumbi* (lidza) *ndikubwerera pansi pomwe linali kale mzimu* (mpweya) *ndikubwerera kwa Mulungu amene anawupereka*” (Mlaliki 12:7). Taonetsa kale kuti Mulungu amapezeka paliponse mwa Mphamvu Yake. Moteronso, “*Mulungu ndi Mzimu*” (Yohane 4:24). Ife tikamafa, timapuma “*mpweya wathu womaliza*” m’njira yomweyi, Mphamvu Ya Mulungu mwaife imakhala ikutichokera. Mzimu umenewu (mpweyawu), umapita ndi kukasungidwa pamodzi ndi mpweya wina wa Mulungu umene ulipo kale pakati pathu, ndi pena paliponse monga tanena kale kuti Mulungu amapezeka paliponse; koteru, “*Mzimu udzabwerera kwa Mulungu*”.

Chifukwa chakuti Mzimu Wa Mulungu ndiwo umayang’anira chilengedwe chonse, ndondomeko yonse ya imfa mwa anthu ndi nyama imatsata njirayi m’mphamvu yake ya mzimuyi. Anthu ndi nyama zonse ziri ndi mzimu, kapena tinene kuti mphamvu kapena moyo wake womwewo mkati mwawo. “*Pakuti chomwe chigwera ana a anthu chigweranso nyamazo; ngakhale chowagwera n’chimodzi modzi; monga winayo angofa momwemonso zinanzo zifanso; inde onsewo ali ndi mpweya umodzi* (mzimu umodzi); *Pakuti munthu sapambana nyama pakuti zonse ndi chabe..*” (Mlaliki 3:19). Timamvanso tikapitirira kuwerenga kuti ndithudi, palibe kusiyana pakati pa malo amene mzimu (mpweya) wa munthu umapita ndinso kumene kumapita mzimu wa nyama (Mlaliki 3:21). Kafotokozedwe ka anthu ndi nyama kuti ziri ndi mzimu umodzi ndipo kuti zonse zimafanso chimodzi modzi, zikuwonekanso kuti pali kufotokoza mobwereza bwereza kuti anthu ndi nyama, zomwe zidaali ndi mzimu umodzi wamoyo ochokera kwa Mulungu (Genesis 2:7; 7:15); zonsezi zinawonongedwa ndi imfa imodzinso nthawi ya Nowa pamene madzi adasefukira: “*Ndipo zinafa zamoyo zonse zoyenda padziko lapansi, zouluka ndi nyama, ndi zamoyo, ndi zokwawa zonse zakukwawa padziko lapansi, ndi anthu onse; zonse zimene m’mphuno zawo munali mpweya* (mzimu) *wamoyo, zonse*

zamoyo padziko lapansi...” (Genesis 7:21-23). Onaninso momwe buku la Masalmo 90:5 likufananizira imfa ndi kusefukira kwa madzi m’nthawi ya Nowa. Tionanso poyera tikawerenga Genesis 7 kuti munthu ndi chimodzi modzi ndi nyama zonse zolengedwa – “zamoyo zonse”. Ichi n’chifukwa chakuti zonse ziri ndi mzimu (mpweya) umodzi omwewo wamoyo wao, monga nyamanso zimakhala nawo mzimu.

4.4 KIPA IMFA NDIKO KUSAPUMA KOMANSO KUSAKUMBUKIRA

Kuchokera m’Phunziro 4.3 tangomalizali pokamba za Mzimu, moyo wa munthu ndi zina zonse, tingatinso taona kuti munthu wakufa amakhala opanda mpweya – samapuma komanso samakumbukira zomwe zinachitika m’moyo wake onse. Pamene ntchito zake zonse zimene adachita ali ndi moyo zimakumbukidwa ndi Mulungu, iye samakumbukira china chirichonse chimene anachita m’moyo wake onse (Mlaliki 3:16; Chibvumbulutso 20: 12; A Hebri 6:10); Izi zikutitsimikiziradi kuti ife tikafa sitikumbuka zomwe tidachita m’moyo wathu kotero, n’koyenera kuti, Mulungu Yekha ndi amene amakumbukira zochita za munthu aliyense iye mwini akafa. Ndime zotsatirazi zikulongosola mwachimvekere nkhani imeneyi:-

- “..(munthu) *mpweya wake uchoka*, (iye) *abwerera kumka ku nthaka yake; Tsiku lomwelo* (nthawi yomweyo) *maganizo ake amatha*” (Masalmo 146:4).
- “...*akufa sadziwa kanthu bi...chikondi chawo, ndi mdano wao, ndi dumbo lao lomwe zatha tsopano*” (Mlaliki 9:5,6). Kulibe “*nzeru kumanda ulikupitako*” (Mlalilki 9:10) – Kulibe maganizidwe ena aliwonse, choncho, kulibenso kupuma monga ena amanenera.

- Yobu akunena za imfa yake kuti **“Ndikadakhala monga ngati sindikadakhala; akadangonditenga pobadwapo kumka nane kumanda...”** (Yobu 10:19). Iye akuti zikanakhala bwino akanangopitirira atabadwa osakhala ndi moyo chifukwa akudziwa kuti munthu wakufa samakumbukira china chirichonse kotero, zomwe anazona iye sakanazionanso kapena kuzikumbukira akanakhala kuti adapitirira osakhala ndi moyo patsiku limene iye anabadwa.
- Munthu amafa monga nyama ina iriyonse imafanso (Mlaliki 3:18); ngati munthu angapulume kuimfa, kwina kwake nyamanso zimatha kupulumuka.
- Mulungu **“..Akumbukira kuti ife ndife mpfumbi koma munthu masiku ake akudza ngati udzu; Aphuka monga duwa la kuthengo...Pakuti mphhepo ikapitapo pakhala palibe: Ndi Malo ake salidziwanso..”** (Masalmo 103:14-16).

Tatsimikizira kuti imfa ndi chizimo cha munthu, sadziwa chochitika, ngakhale oyera mtima sadziwa kanthu. Tiwerenganso kuti ana a Mulungu omwe ankamukhulupirira, ankapempha Mulungu wao kuti apitirize kuwaonjezera masiku a moyo wao n'cholinga chakuti amupembedzebe, chifukwa ankadziwa kuti akangofa, sadzakhanso ndi mwayi otere pozindikiranso kuti wakufa sadziwa kanthu za izi. Hezekiya (Yeseya 38:17-19) ndi Davide (Masalmo 6:4,5; 30:9; 39:13; 115:17) ndi zitsanzo zina za anthu a Chiuta omwe anapempha Yehova Mulungu kuti awaonjezere nthawi ya miyoyo yawo. Imfa kawiri kawiri, ikukambidwa ngati kugona tulo tosatha chabe kapena kupuma kwa onse ochimwa ndi osachimwa (Yobu 3:11,13,17; Danieli 12:13).

Apa taonera limodzi kuti sizoonanso kuti oyera mtima akafa, amapita kumalo a chisangalalo ndi kukalandira mphatso kumwamba ayi, izi sitingazipeze pena paliponse m'Baibulo. Chiphunzitsa choonadi cha uthunthu weni weni wa munthu ndi zoonanso zake zeni zeni za imfa m'Baibulo zimatipatsa chilimbitso champhamvu ndi mtendere m'mitima mwathu. Munthu ataona mabvuto osiyana siyana, ndi zowawa zambiri m'moyo uno mpaka pamene amapita kumanda, samakumbukira kanthu kena kalikonse pa zinthu zonse zimene anazionazo. Ndipo ena onse omwe sanamvepo kapena kuti anafa osadziwa za Uthenga

Wabwino, komanso kuti sakudziwa zofuna za Mulungu pa moyo wathu iwo sadzalandira chiweruzo china chirichonse. Zonse zobvuta zamoyo uno, zowawa ndi zopinga pinga kwa iwo, sizidzaonekanso. Chiyembekezo chonse chabodza, ndi mantha awo opanda pake, sadzaonekanso.

M'maphunziro a Baibulo ambiri, timapezamo njira zambiri zoti tingadziwe choonadi, komabe, zomvetsa chisoni kuti palinso njira zina zosalongosoka pa chipembedzo choonadi, choyenera, popeza anthu ambiri samakhala ndi chidwi chophunzira Baibulo kokwanira. Izi ndi zomwe zidabweretsa chisokonezo pa kamwedwe komanso kamasuliridwe ka Mau Oyera m'Baibulo. Moteronso, munthu lero amaganiza kuti iyeyo samafa ayi, kapena kuti palibe mbali ina ya thupi lake yomwe siimaferatu ayi; koma kuti amapita kumalo ena ake kumwamba iye akangofa. Munthu akafika pokhulupirira zimenezi, amaoneratu kuti akafa, adzapita kumalo ena abwino kapena oyipa amene ali kumwamba (heaven), kumene kumapita onse ochita bwino kapena kuyipa malingana ndi m'mene ankakhalira umoyo wao padziko lapansi lino. Malo amenewa iwo amati ndi kumwamba (heaven) kumene kumapita onse ochita zabwino; ndinso 'Hade' komwe kumapita onse ochita zoyipa pamaso pa Mulungu. Taona kale kuti munthu akafa, palibenso gawo lina lirilonse la thunthu la munthu lomwe limakhalabe ndi moyo; Baibulo silikambapo kanthu kena kalikonse pokhudza za munthu amene amapita kumwamba. Mfundo zina zimene zirinso zabodza tikumbutsanabe pofuna kupitiriza mwachindunji phunziro lathu lino. Pakali pano, tiyeni tipitirize kunena kuti sizoono:-

- Kutu mphotho ya muyaya imaperekedwa kwaife popeza tiri ndi mzimu umene sumafa ndipo kuti mzimu'wo umapita kumalo ena ake pamene munthuyo wafa.
- Kutu anthu ochimwa ndi oyera mtima amapatulidwa pa tsiku limene iwo amafa.
- Kutu mphotho ya oyera mtima ndiyo kupita Kumwamba.
- Kutu ngati aliyense ali ndi "mzimu" womwe sumafa, ndiye kuti aliyense ayenera kupita Kumwamba kapena kumalo a mazunzo.

- Kuti anthu onse ochimwa mizimu yawo idzapita kumalo a chilango chosatha otchedwa “hell” kapena kuti “hade” – malo a chilango choopsa.

Timvetse kuti sicholinga chathu kumangoonetsa maganizo otsutsa okha okha pa mitu yalembedwa’yi ayi; Tifuna tipemphe kuti kuchita zinthu zirizonse moganizira mfundo zimene ziri pamwambazi mwatsatane tsatane, pofufuza zoona zake zeni zeni kuchokera m’Baibulo, lomwe lingatiwunikire popeza ndiwo Mau a Mulungu, n’kofunikira. Kotero, tikupemphani tsopano kuti mufufuze nokha poganizira ndime zomwe mwapatsidwa potsimikizira mfundo ndi ndondomeko zimenezi.

4.5 KUUKANSO KWA AKUFA

Baibulo limatitsimikizira kuti mphotho ya oyera mtima idzaperekedwa pamene anthu adzawukitsidwa kwa akufa, komanso pamene Khristu adzabweranso kuchokera kumwamba (1 Atesalonika 4:16). Kuukitsidwa kwa anthu kwa akufa (onani Phunziro 4.8) ndicho chinthu choyambirira kuchitika ndi Khristu kenaka; kudzakhala chiweruzo cha ntchito za anthu amene ankazindikira komanso adamvapo Uthenga Wabwino.

Zikadakhala kuti mzimu umapita kumwamba munthu akafa, ndiye kuti kuukitsidwa kwa anthu pa tsiku lobwera Khristu sikudzakhala kofunikira. Paulo ananena kuti ngati kulibe kuukitsidwa kwa akufa, ndiye kuti sikoyenera kwa munthu kumvera Mulungu (1 Akorinto 15:32). Tiona kuti Paulo sakananena chonchi akanakhala kuti chikhulupiriro chake ndicho kudzapita kumwamba mu mzimu wake (kanthu kosafa) kuti akalandire mphotho ya moyo wosatha akadzangofa. Koma nanga ngati iye ali wosafa akalandira bwanji moyo wosathawo? Tiganizire kuti ngati munthu angapite kumwamba ali ndi moyo wake, sizingakhale zomveka kuti akalandirenso moyo wina. Zoona zake apa ndi

zakuti iye (Paulo) ankakhulupirira kuti kuukanso kwa thupi la munthu kwa akufa ndicho chiyambi cholandira mphotho ya moyo wosatha kwa munthu olungama patsiku lomaliza'lo, komanso kuti ndiyo mphotho yokhayo imene m'khristu aliyense ayenera kuiyembekezera monga mwamalonjezano m'malembu. Yesu Khristu anatilimbikitsa kuti tikhale ndi chiyembekezo m'chikhulupiriro chathu mwa Iye m'moyo wathu onse kutidi "tidzaukitsidwe kwa akufa" patsiku'lo (Luka 14:14).

Tidziwe kuti munthu (kapena chinthu china chirichonse chimene chimatchedwa chinthu chimadziwika) adziwika kuti ndi munthu chifukwa cha maonekedwe ndi uthunthu wake m'thupi lomwe amakhala nalo. Ichinso ndi chimodzi modzi Mulungu, Yesu Khristu, Angelo ndi anthu onse amene alinso ndi uthunthu wao-wao. Yesu akadzabwera, "...*adzasanduliza thupi lathu lopepudwa, kuti lidzafanane nalo thupi lake la ulemero*" (Afilipi 3:20,21). Monga lero Khristu ali ndi thupi mu uthunthu wake, limene liri ndi mphamvu ya Mzimu Woyera osati mwazi, ifenso matupi athu adzakhala monga thupi la Khristu lomwe ali nalo lero, ndipo iyi ndiyo mphatso yathu yomwe tonse tiyenera kuiyembekezera. Mphotho imeneyi tidzalandira mogwirizana ndi m'mene umoyo wathu unaliri m'thupi la moyo uno (2 Akorinto 5:10).

Onse omwe pa nthawiyo adzakhala mtchimo, kapena adzafa m'chikhalidwe chao cha uchimo, adzasiyidwa m'thupi lawo lomwelo la uchimolo mpaka adzawola; nkubwerera ku mpfumbi; Pamene onse omwe m'thupi lawo la umoyo uno, adayesetsa ndipo panopa ngati ali ndi moyo akuyesetsa kukhala nawo umoyo odziletsa, oyesa yesa kuchita chifuniro cha Ambuye wao, monga Mzimu wa Mulungu umafunira, "...*Chochokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha*" (Agalatiya 6:8) mu uthunthu wa thupi lodzozedwa ndi Mzimu.

Pali umboni wokwanira kuti mphotho ya moyo wosatha idzaperekedwadi mu uthunthu wa thupi limene tiri nalo'li. Tikangomvetsa ndi kubvomereza zonsezi, tiona kufunikira kwake kwa kuukanso kwa thupi lathuli pamene tidzawukitsidwe kwa akufa. Thupi lathuli limatha tikangofa; lonjezo lokhala ndi moyo wosatha m'thupi, ndi lomveka bwino kotero kuti, wakufa samadziwadi chirichonse pokha pokha ngati thupi lakelo litakonzedwanso komanso kuti munthuyo atawukitsidwa kwa akufa napatsidwanso maonekedwe a Mulungu.

Buku lonse la 1 Akorinto 15 likufotokoza nwandondomeko yomveka bwino ya kuukanso kwa akufa; Tikawerenga mofatsa ndime zonse, tiona kuti ndi yopindulitsa koposa ndikuti titha kumvetsa bwino pa mutu umenewu wa kuukanso kwa akufa. 1 Akorinto 15:35-44 Paulo akufotokoza kuti mbeu ikabzalidwa m'nthaka, imamera kenaka imapatsidwa uthunthu'wu (thupi) ndi Mulungu; Ndipo mwanjira yomweyi, ngati momwe mbeu yopanda uthunthu imapatsidwa uthunthu'wu ndi Mulungu, anthu akufa mchizindikiro chake adzapatsidwanso thunthu lawo patsiku lowukitsidwalo, nalandira mphothoyo mu uthunthu waowo. Monga Khristu anawuka kuchokera mdzenje la manda, ndinso monga thupi lake linasinthidwa kukhalanso losafanso, ifenso tikakhulupirika ngati Khristu, tidzawukitsidwa komanso thupi lathu lidzakhala losinthika (Afilipi 3:21). Mu ubatizo, ife timadzilumikiza kuimfa ya Khristu ndi kuukanso kwa akufa; Timatsimikizira chikondi ndi chikhulupiriro chathu kuti ndithu tidzalandira nawo mphotho ya malonjezano imene Khristu'yo anali woyamba kuyilandira poukanso kwa akufa (Aroma 6:3-5).

Tikabvutika monga Khristu anabvutikira, ndiye kuti tidzalandira mphotho yomwenso Khristu'yo analandira: *“...nthawi zonse tirikusenza senza m'thupi kufa kwake kwa Yesu, kuti moyonso wa Yesu uoneke m'thupi mwathu”* (2 Akorinto 4:10). *“...Iye amene adaukitsa Yesu Khristu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa mzimu wake wakukhala mwa inu”* (Aroma 8:11). Mchiyembekezo chimenechi, ife kotero, tiyenera kudikira molimba mtima *“chiomboledwe cha thupi lathu”* (Aroma 8: 23) kudzera m'thupi limene silidzafanso.

Chiyembekezo chodzaukitsidwanso kwa akufa, kuti tidzakhale ndi moyo wamuyaya m'thupi monga mwa chiyembekezo ndi mfundo imene ana a Mulungu m'wasiku oyambirira akhala akuchidikirira. Abrahamu anawuzidwa kuti iye adzakhala mwini nthaka wa dziko la Kanani nthawi zonse, mpaka muyaya pomwe iye ankayendera dziko lonselo (Genesis 13: 17; onaninso Phunziro 3.4). Apa tiona kuti Abrahamu anakhulupirira kuti thupi lake lidzaukitsidwa mtsogolomo, nakhalanso ndi moyo wamuyaya kotero, m'njira imeneyi, zonsezi zidzakwaniritsidwa.

Yobu analongosola mwachindunji m'mene iye anadziwira za mfundo imeneyi ngakhale kuti thupi lake lidaadyedwa ndi nyongolotsi m'manda; iye anadziwa kuti adzalandira mphothoyo mu uthunthu wake mogwirizana ndi Mau a Mulungu: ***“Koma ndidziwa kuti mombolo wanga ali ndi moyo, Nadzauka potsiriza pampfumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, pamenepo ndidzampenya*** (m'thupi langa ndekha) ***ndekha, Ndimanso anga adzamuona, siwina ayi,***” (Yobu 19:25-27). Chiyembekezo cha Yesaya sichidali chosiyana ndi m'mene aneneri ena monga Yobu ankadziwira za mfundo imeneyi: ***“..thupi langa, ngakhale likhale mpfumbi, lidzauka...”*** (Yesaya 26:19).

- Mau ofanana ndi amenewa amafotokozerwa momveka kwambiri pamene nkhanu ya imfa ya Lazaro yemwe anali okondeka wa Yesu Khristu inalembedwa. Mnkhanu imeneyi, timamva kuti m'malo mopepesa komanso kutonthoza azichemwali ake a Lazaro za imfayi, ponena kuti Lazaro uja mizimu wake wapita kumwamba, Yesu anawalongosolera za tsiku lomwe iye (Lazaro) adzaukitsidwe kwa akufa: ***“...Mlongo wako adzauka...”*** Momwe anayankhira Marita, m'chemwali wake wa Lazaro, akuonetseratu kuti mbiri ya kuukanso kwa akufa kwa anthu, ndi zinthu zimene a khristu akale masiku amenewo ankadziwa komanso ankayembekezera patsiku lobweranso kwa Ambuye Yesu Khristu. ***“Marita ananena ndi Iye, Ndidziwa kuti adzauka m'kuuka tsiku lomaliza”*** (Yohane 11:23,24). Tikaganizira monga Yobu wakhala akunenera, Marita nayenso anali asanamvepo kuti imfa ndi chitseko chimene chimatseguka kutitengera ife ku moyo wina wachisangalalo kumwamba kwa Mulungu ngati momwe ena amanenera. Ndiponso sanadziwepo za malo amene Mulungu anakhazikitsa kumwamba kuti anthu olungama akasangalaleko ndi za malo a chionongeko kumene anthu oyipa akaonongeka kumoto osatha koteru, dziko lapansi lidzaphwasulidwa ayi. Izi tikaona zikusiyana kwambiri ndi zimene anthu tikupempha mpemphero la Ambuye Wathu Yesu Khristu ***“...ufumu wanu udze*** (udze padziko lapansi lino [Mateyu 6:9-13])”.
- ***“..Odala ali akufatsa; chifukwa adzalandira dziko lapansi”*** (Mateyu 5:5) osati kuti ***“...chifukwa mizimu yawo idzapita kumwamba ayi”***. Izi zikugwirizana ndi zomwe timawerenga pa Masalmo 37 pomwe

timamva motsimikizira kuti mphotho ya oyera mtima idzaperekedwa pansu pano. Awa ndi malo omwe anthu ochimwa akhala akusangalalapo kwa nthawi yaitali, namalamulira anthu anzawo mwankhaza, posankhana mitundu komanso ndi chinyengo. Malo amenewa ndi omwe padzakhale bwalo la chiweruzo, kenaka kuperekedwa kwa mphotho ya moyo wosatha kwa anthu ochita chilungamo pamaso pa Yehova koteru, iwo adzalandira, nakhala eni ake eni eni a dziko lapansi (Masalmo 37:34,35). **“Ofatsa adzalandira dziko lapansi; Nadzakondwera nawo mtendere wochuluka ..Pakuti iwo amene awadalitsa adzalandira dziko lapansi...olungama adzalandira dziko lapansi, Nadzakhala momwemo kosatha”** (Masalmo 37:11,22,29). Kukhala padziko lapansi/dziko lamalonjezano kosatha kutanthauza kuti palibenso zoti anthu adzapita kumwamba, izi sizidzakhala choncho koteru, anthu amene amalalikira zimenezi amatsutsana ndi chiphunzitsu cheni cheni cha Mulungu Mwini monga tawerenga tokha m’Buku Loyera.

- **“Davide..kuti adamwalira naikidwanso, ndipo manda ake ali ndi ife kufikira lero lino...Davide sanakwera Kumwamba ai,”** (Machitidwe 2:29,34). M’ malo mwake, Petro akunenetsa kuti chiyembekezo chake cha Davide chidatsamira pa mutu wakuti adzaukanso kwa akufa pamene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri padziko lino lapansi. (Machitidwe 2:22-36).
- Dziko lapansi ndi malo amene Mulungu anakonza kuti akakwaniritse zochita zake ndi anthu: **“...Kunena za Kumwamba, Kumwamba ndiko kwa Yehova; Koma dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu”** (Masalmo 115:16).
- Chibvumbulutso 5:9,10 akukamba za masomphenya a anthu oyera mtima, amene ali okhulupirika kuti adzanena/adzachita chiyani patsiku la chiweruzo pamaso pa Yesu pamene adzakhale pa Chimpando wa Chifumu Wake. Monyadira, iwo adzanena: (Khristu) **“mudawayesa** (mudawapanga) **iwo ufumu** (alamulire) **padziko** (lapansi)”. Ngakhale Baibulo la Chichewa lidamasuliridwa molakwika, apa chachikulu ndi chakuti “oyera mtima onse adzapatsidwa mwayi olamulira dziko lonse

lapansi mpaka muyaya; Ndipo izi zikusiyana kwambiri ndi ulaliki oti tidzapita Kumwamba tikadzafa” – Nanga ulamuliro wathu wa dziko lapansi monga Baibulo likunenera udzachitika liti?

- Maulosi a Danieli m’manusu 2 ndi 7, amakamba za kusintha kwa maulamuliro pa ndale m’dziko lapansi zomwe kothera kwake, kudzakhala kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu pamene Khristu adzabwerenso pansi pano. Ufumu wa Mulungu umenewu udzakhazikitsidwa **“pansi pa ulamuliro wochokera Kumwamba”**.
- Ndipo udzafala ndikudzaza **“mdziko lonse lapansi”** (Danieli 7:27; 2:35 cp. Ndime 44). Ufumu wosatha wa Mulungu ndi ulamuliro umenewu **“zidzapatsidwa kwa anthu opatulika a Mwambamwamba** (Danieli 7:27); Mphatso yawo kotero, ndiyo moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu omwe udzakhazikitsidwe pansi pano – pansi pa Kumwamba Mwamba.

4.6 CHIWERUZO

Chiphunzitso cha Baibulo pa mutu wa chiweruzo chirinkudzacho, ndi umodzi mwa mitu yambiri ya Mau a Mulungu yomwe imayenera kudziwidwa ndi munthu aliyense pamene asanalandire ubatizo (Machitidwe 24:25; A Hebri 6:2). Kawiri kawiri Mau Oyera akukamba za “tsiku la chiweruzo” (mwachitsanzo, 2 Petro 2:9; 3:7; 1 Yohane 4:17; Yuda 6); nthawi iyi ndi yomwe onse omwe amadziwa Mau a Mulungu adzalandire mphotho. Onsewa adzayenera **“kuyima kumpando wakuweruza wa Mulungu”** (Aroma 14:10), kotero **“Pakuti ifenso tonse tiyenera kuwonekera kumpando wa kuweruza wa Khristu”** (2 Akorinto 5:10); kuti tikalandire mphotho ya moyo wathu pamene tsiku’li likadzafika mogwirizana ndi m’mene moyo wathu wa dziko lino lapansi unaliri m’thupi lathu lino.

Masomphenya a Danieli ponena zakubweranso kachiwiri kwa Khristu, anaphatikizapo chiweruzo cha Khristu pampando wake wa Chimfumu (Danieli 7:9-14). Mafanizo a Yesu m'Baibulo m'mitu yosiyana siyana angathandizenso kuti tizindikire zinthu zambiri zokhudza choonadi. Chitsanzo cha fanizo la materente likufananizidwa ndi kubweranso kwa Ambuye Yesu, pamene adzafunse okhulupirira Mau a Mulungu ndi kuwaweruzo monga iwo anachitira; kuwengeretsa zonse zomwe iwo anakhoza kuchita kapena kulakwitsa monga mwamalamulo; ngati iwo analondoloza kapena ayi mogwirizana ndi malangizo a Yehova (Mateyu 25:14-29). Fanizo la khoka la nsomba lifanana ndi anthu omwe akuwedza nsomba, polalikira Uthenga Wabwino kwa anthu; Ndipo anthu omvera afanana ndi nsomba zokodwa m'maukonde osiyana siyana, mwachitsanzo, lero tiri ndi matcharitchi ambiri amene ena ambirinso samalalikira Uthenga weni weni woonadi. Mfanizo limeneri, tiona kuti anthu aja akukhala pansu kusankha nsomba zabwino ndi zoyipa kenaka akuzigawa m'magulu awo (chimodzi modzi tsiku lomaliza la chiweruzo, anthu adzasankhidwa m'magulu awiri amenewa) monga iwo anachita komanso mogwirizana ndi Uthenga Wabwino umene anawumvawo (Mateyu 13:47-49). Kumasulira kwa mtundu wotere ndikosabvuta chifukwa kumatizindikiritisa Mau ake m'choonadi kuti ***“...Padzatero pa chimaliziro cha nthawi ya moyo uno pansu pano: angelo adzatuluka, nadzawasankhula oyipa pakati pa abwino”***.

Tikatenga zomwe tawona tsopano, tidziwa kuti Yesu akadzabweranso, ndi kuti anthu akadzaukitsidwanso kwa akufa, anthu onse omwe anamva Uthenga Wabwino adzasonkhana kukakumana ndi Ambuye. Aliyense adzawunikidwa monga mwa ntchito zake kotero, mphotho idzaperekedwa kwa okhawa ochita bwino pakumalizidwa kwa chiweruzo. Fanizo la nkhusa ndi mbuzi likutsindikanso pa mfundo yomweyi: ***“Mwana wa munthu adzadza mu ulemerero wake, ndi angelo onse pamodzi naye, pomwepo Iye adzakhala pa Chimpando chakuwala kwake”*** (mpando wa chifumu wa Davide bambo wake mu mzinda wa Yerusalemu, Luka 1:32,33); ndipo adzasonkhanitsa pamaso pake anthu amitundu yonse (Mwachitsanzo, anthu ochokera m'mayiko onse padziko lonse, cp. Mateyu 28:19); ***“ndipo Iye adzawalekanitsa iwo wina ndi mzake, monga mbusa alekanitsa nkhusa ndi mbuzi; nadzakhaliitsa nkhusa kudzanja lamanja, koma mbuzi kudzanja la kumanzere. Pomwepo Mfumuyo (Yesu) idzanena kwa iwo akudzanja la manja, Idzani kuno inu odalitsika a***

Atate wanga, lowani mu ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi” (Mateyu 25:31-34).

Kukhala mu Ufumu wa Mulungu, ndiko kulandira malonjezano a Abrahamu okhudza Ufumu’wo, chotsatira chake cha mphotho yokhala nawo moyo wosatha. Zonse timamva kuti zidzachitika patangotha chiweruzo, iyi ndi nthawi imene Khristu adzaweruzwa anthu ake patsiku lomaliza akadzabweranso pansi pano. Choncho, tizindikire kuti ndi kobvuta lero lino kulandira mphotho ya moyo imeneyi pamene Ambuye Yesu Khristu asanabwere padziko lapansi; Apa timalize ponena kuti pamene munthu amafa, mpaka nthawi imene adzaukitsidwe kwa akufa, iye samadziwa kanthu kena kalikonse, ndipo kuti samakhala nacho chikumbukiro cha zomwe zinachitika m’moyo wake popeza kuti, ndi kobvuta kuti ichi chichitike mwayiye chifukwa thupi lakelo, liribe mphamvu ya Mulungu monga linaliri kale. Mphamvu ya Mulungu ikachotsedwa mwaife, chikumbukiro chathu chonse chimachoka.

Kawiri kawiri Baibulo limatitsimikizira kuti tidzalandira mphotho yathu ya malonjezano pamene Khristu adzabwere pansi pano basi—osati lero kapena tikafa Iye asanabwere ayi:-

- *“Ndipo pakuonekera Mbusa Wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero”* (1 Petro 5:4 cp. 1:13).
- *“Khristu Yesu...amene adzaweruzwa a moyo ndi akufa ndi pamaonekedwe ake ndi Ufumu Wake...chotsatira wandiyikira ine korona wa chilungamo, amene Ambuye woweruzwa wolungama adzandipatse ine tsiku lijalo”* (2 Timoteo 4:1,8).
- Patsiku lomaliza la Mpulumutsi Mesiya, *“..ambiri a iwo ogona mpfumbi lapansi* (Genesis 3:19) *adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena kumanyazi ndi m’nyozo wosatha* (care translation errors from English to Chichewa [Danieli 12:2])”

- Pamene Khristu adzabweranso kudzaweruza, onse *“ali m’manda adzamva mau ake, nadzatulukira, amene adachita zabwino ku kuuka kwa moyo; koma amene adachita zoyipa ku kuuka kwaimfu”* (Yohane 5:25-29).
- *“...Ndidza (Yesu) msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake”* (Chibvumbulutso 22:12). Sitiyenera kuti tipite kumwamba kukalandira mphotho ayi, koma kuti monga mwa Mau a Baibulo, Yesu Khristu adzabwera monga ananena, kudzatipatsa ife tonse moyo kuchokera kumwambako:

Kubweretsa mphotho kwa Khristu Yesu, kukutanthauza kuti mphotho’yo inakonzedwa kale kumwambako ndipo kuti Khristu adzabwera pansu pano pamene Iye adzabweranso kachiwiri; Kulandiridwa kwa dziko lamalonjezanso a dziko lapansi lino amene adapangidwa pakati pa Mulungu ndi kholo lathu Abrahamu m’njira iyi, *“Kuti tilandire cholowa chosabvunda ndi chosadetsa ndi chosafa, chosungikira m’Mwamba inu, amene musungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa chikhulupiriro, kufikira chipulumutso chokonzeka kukabvumbulutsidwa nthawi yotsiriza* (1 Petro 1:4,5).

Tikalola izi mozindikira, mogonja komanso molakalaka kudziwadi Mau Ake Oyerawo, tidzatha kumasulira bwino mopanda chisokonezo china chirichonse pa ndime ya Yohane 14:2,3: *“..ndipita (Yesu) kukakukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzerani inu malo* (mphotho “yosungidwa kumwamba”), *ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwaine ndekha; Kuti kumene kuli ineko, mukakhale inunso”*. Tikamawerenga malo ena m’Baibulo, timamva kuti Yesu ananena kuti adzabweranso kudzatipatsa mphotho (Chibvumbulutso 22:12), ndipo tawona kuti mphothoyi idzaperekedwa patsiku lomwe Iye adzabweranso kudzaweruza nakhala pa Chimpano cha Chifumu cha atate Wake Davide. Khristu adzalamulira pa mpando wa Chifumu wa bambo Wake Davide umene kalelo udali mu Mzinda wa Yerusalemu “mpaka muyaya” (Luka 1:32,33). Iye adzakhala pa Ufumu’wo mpaka muyaya omwe udzakhazikitsidwe padziko lapansi, muulamuliro Wake wa Ufumu wa Mulungu, ifenso tidzakhala komweko (Yohane 14). Lonjezo lake *“ndidzalandira inu kwaine ndekha”* choncho, tingalizindikire kuti Iye adzatipatsa kapena tinenenso kuti adzatilandira

pa tsiku la chiweruzo. Liwu’li m’chi Greek, *“ndidzalandira inu kwaine ndekha”* likugwiritsidwanso ntchito pa Mateyu 1:20 pamene Yosefe *“anatenga (Mariya) kwa iye yekha”* ngati mkazi wake. Kotero mwaichi, sikutanthawuza kuti ife tidzapita kwa Yesu kumwamba ayi. Iye adzalandira ife kwa Iye Yekha pamene adzakhazikitse Ufumu Wa Mulungu panso pano.

Monga tawona kuti mphotho idzaperekedwa pa tsiku la chiweruzo lokha pamene Khristu adzabweranso, ndizoonekeratu kuti onse oyera mtima ndi ochimwa akafa amapita kumalo amodzi – ndiwo kumanda. Imfa ya anthu ochimwa ndi ya anthu oyera mitima siimasiyana ayi. Ndime zotsatirazi ndi zimene zikupereka chitsimikizo cha nkhani imene tikunena panoyi:

- Yonatani anali oyera mtima pamene Sauli anali ochimwa ngakhale kuti *“...Ndipo m’imfa yawo sanasiyana; ”* (2 Samueli 1:23).
- Sauli, Yonatani ndi Samueli onse anapita kumalo amodzi atafa – ndiko kumanda (1 Samueli 28:19).
- Abrahamu yemwe anali oyera mtima a *“..natengedwa nakhala ndi mtundu wake”* kapena tinene kuti makolo ndi abale ake pamene iye anafa; iwo (makolo ake) anali opembedza mafano koma onse anakhala pamodzi kumandako mpaka lero (Genesis 25:8; Yoswa 24:2).
- Opusa mu uzimu ndi ochenjera mu uzimu onse amafa imfa imodzi osati yosiyana ayi koma imfa yofanana (Mlaliki 2:15,16).

Zonsezi tidziwa zikusiyana kwambiri ndi zimene a khristu ambiri a lero lino amanena komanso kukhulupirira. Iwo amanena kuti oyera mtima amapita kumwamba akafa ndipo izi zimasiyana ndi chikhulupiriro cheni cheni choonadi cha Baibulo, chimene chimatiphunzitsa kuti; onse amene adazindikira chilongosoko cha Uthenga Wabwino, adzaukanso kwa akufa ndikuti adzaweruzidwa pamene Khristu adzabwerenso. Izi taonanso kuti ndi zinthu zofunikira kwathunthu pa chipulumutso chathu, choncho, mu Uthenga Wabwino ndizofunikiranso kuzidziwa mwachimvekere mosachotsa kapena kuyikapo kanthu kena kalikonse. Mwanjira imeneyi, tiona kuti munthu oyera mtima

akafa, saamapita kumwamba kukalandira mphotho ayi; Komanso sizoono kuti ena onse amene amafa pambuyo pake amakamupeza Kumwamba munthu wakufayo iwo akadzafanso nakalandiranso mphotho zawo ayi. Tawoneratu kuti adzasonkhanitsidwa pamodzi patsiku lomaliza pamene Khristu adzabweranso naweruza onse padziko lapansi lino.

- Nkhosa zidasankhidwa imodzi imodzi kuchokera m'chigulu cha mbuzi patsiku la chiweruzo. Pakutha kwa chiweruzo, Khristu adzanena kwa nkhosa zonse zosonkhana ku dzanja lake la manja kuti :-

“Idzani kuno inu odalitsika a Atate anga, landirani Ufumu wokonzedwa kwainu” (Mateyu 25:34). Mwaichi, nkhosa zonse zidzalandira mphotho ya Ufumuwo nthawi imodzi yomweyo (cp. 1 Akorinto 15:52).

- **“Pokolola”** pamene Khristu adzabweranso kudzaweruza anthu onse; onse amene anadzipereka polalikira Uthenga Wabwino **“adzasangalala pamodzi”** (Yohane 4:35,36 cp. Mateyu 13:39).
- Chibvumbulutso 11:18 akunena za **“nthawi ya akufa yomwe iwo adzaweruzidwa”** ngati kuti ndi nthawi yomwe Mulungu adza **“pereke mphotho kwa akapolo anu aneneriwo...ndi oyera mtima...iwo akuopa dzina lanu”** Mwachitsanzo, onse okhulupirira pamodzi.
- A Heberi 11 ndi nunsu ina mwa manunsu ambiri omwe akutchula maina a anthu m'Chipangano Chakale – amene adachita bwino pamaso pa Chiuta. Ndime ya 13 ikuthirira ndemanga iyi **“...Iwo onse adamwalira m'chikhulupiro, osalandira malonjezano,”** **“omwe anapangidwa kwa Abrahamu** (pakati pa Mulungu ndi Abrahamu), **polowa mu Ufumu wa Mulungu** (A Heberi 11:8-12).

Apa zikuonekeratu kuti anthu onsewa sanapite kumwamba m'modzi m'modzi payekha, kuti akalandire mphotho zawo monga anthu ena amanenera za anthu akufa kuti amapita kumwamba. Chifukwa chimene izi zonse sizinachitike mwachomwechi chikuperekedwa pa ndime zotsatira za

39,40: Iwo onse *“adamwalira m’chikhulupiriro osalandira malonjezano: Mulungu popereka zinthu zabwino, kwaife, popeza Mulungu adatikonzera ife kanthu koposa, kuti iwo asayesedwe a mphumphu opanda ife”*.

Cholinga chimene Mulungu anachedwetsera kupereka mphotho zawo monga mwamalonjezanowo, chinali chifukwa chakuti idaali ndondomeko ndi chikonzero chake cha Mwini Yehovayo kuti zinthu zidzakhala motere panthawi anayikonzayo; Choncho, onse okhulupirira *“akhale oyera ndi amphumphu”* pamodzi ndi anzawo ena onse panthawi imodzi yomweyo osati yosiyana ndi ena ayi. Iyi ndiyo nthawi yomwe Khristu adzatiweruze akadzabweranso padziko lapansi lino.

4.7 MALO OLANDIRIRA MPHOTHO: Kumwamba Kapena Pansi?

Mongoganizirapo zifukwa ndi mpfundo zapatsidwa kalezo, mwina ena akuganizabe kuti Kumwamba ndikumene kungakhazikitsidwe kapena kuti kunasankhidwa ndi Yehova ngati malo oyenera kudzakhhalako Ufumu wa Mulungu; mwachitsanzo, malo olandirirako mphotho ya moyo wosatha wamuyaya, anthu amene akukanirirabe ndi maganizo ngati amenewa ayenera atifotokozere momveka bwino bwino zomwe iwo amadziwa pa matanthawuzo a ndime ndinso mpfundo ziri m’munsi:-

- i. **“Pemphero la Ambuye Wathu”** lomwe Yesu Khristu anatiphunzitsa kuti tiyenera kupemphera motere; **“Ufumu Wanu udze,”** mwachitsanzo, pamene Khristu adzabwerenso pansi pano ndi Ufumu wa Mulungu, pofuna kukwaniritsa zomwe Mulungu Yehova anafuna kuti **“Kuchitike monga (zikuchitikira lero) Kumwamba chomwecho pansi pano”** zidzachitikenso momwemo! (Mateyu 6:10). Choncho, ife tonse lero timapempherera kuti Ufumu wa Mulungu Mphambe, udze padziko lino lapansi monga Khristu anatiphunzitsira. Tiyenera kuona tsopano kuti ndi zomvetsa chisoni kumva a khristu mazana mazana akupempherera chinthu choti chidzachitike koma sakudziwa chimene akupempha. Mpemphero’li, iwo ngakhale amapempha motero, samazindikira kweni kweni chomwe akunena chifukwa cha ziphunzitsa zabodza zomwe zayala mizu yolimba m’mitima ndi m’matcharitchi athu a makono. Zikhulupiro zawo ndi zakuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa kumwamba zomwe ziri zosiyana kwambiri ndi chikonzero cha moyo wosatha umene unakhudzanso onse a banja lake: **“...zoonadi nyumba yanga siikhala yotere ndi Mulungu; Koma Iye anapangana ndi ine pangano losatha;”** (2 Samueli 23:5).
- ii. **“Odala ali a chisoni** (ofatsa opirira) **chifukwa adzalandira dziko lapansi”** (Mateyu 5:5) osati kuti “popeza mizimu yawo idzapita kumwamba” ayi. Izi zigwirizananso ndi Masalmo 37, Poona kuti ndime yonse ya Masalmo 37 ikuneneratu kuti mphotho ya olungama idzaperekedwa padziko lapansi pompano. Monga m’mene ochita zoyipa akusangalala padziko lino lapansi lerolino, olungama adzasangalalanso, nalandira ulamuliro wadziko lonse lapansi limene anthu ochimwa linali lawo (Masalmo 37:34,35). **“Koma ofatsa adzalandira dziko lapansi.....Pakuti iwo amene awadalitsa adzalandira dziko lapansi;...olungama adzalandira dziko lapansi nadzakhala momwemo kosatha”** (Masalmo 37:11,22,29). Kukhala m’dziko lapansi (lamalonjezano) nthawi yonse kosatha, ndilo lonjezo la Yehova, apa zikutanthawuza kuti okhalawo adzakhalamo ndi moyo wosatha kosalekeza. Tionetsetse

kuti apa sakuti moyo wosatha kumwamba ayi koma padziko lapansi lino kosatha komanso kosalekeza!

- iii. ***“Davide...kuti adamwalira nayikidwanso, ndipo manda ake ali ndi ife kufikira lero lino” “Pakuti Davide sanakwera kumwamba ayi,”*** (Machitidwe 2:29,34). M’ malo mwake Petro anafotokozera kuti motero, Davide adakhulupirira kuti adzaukitsidwa kwa akufa pamene Khristu adzabweranso (Machitidwe 2:22-36).
- iv. Dziko lapansi ndiwo malo okhawa amene ntchito ya Mulungu imawonekera kwa anthu omwe amakhalamo; ***“Kunena za kumwamba, kumwamba ndiko kwa Yehova; Koma dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu”*** (Masalmo 115:16).
- v. Chibvumbulutso 5:9-10 chikuonetsa chithunzi thunzi chimene olungama angadzakhale nacho pamene adzaloledwe kuonekera pa Mpando wa Chimfumu wa Chiweruzo: ***“(…mudawayesa iwo ufumu ndi ansembe kwa Mulungu wathu; ndipo achita ufumu padziko”*** (note translation errors) Chithunzi thunzi chimenechi cha olungama kuti adzalandira dziko lapansi, chinachotsedwa pakati pa maulaliki a akhristu ambiri lero lino ngakhale kuti Baibulo likutero pa mutu umenewu.
- vi. Maulosi a Danieli 2 ndi 7 akunenetsa polosera kuti maudindo a padziko lapansi lino adzatsagana ndi maudindo anzake a dziko lapansinso mpaka komalizira pamene Ufumu wa Mulungu, udzakhazikitsidwe pobweranso kwa Khristu padziko lino lapansi. Ndipo Ufumu umenewu ***“udzakwanira padziko lonse lapansi”*** nudzaza mdziko lonse (Danieli 7:27; 2:35 cp. v.44); Ufumu wosatha umenewu ***“...zidzapatsidwa kwa anthu opatulika a wa m’mwamba mwamba; Ufumu Wake ndiwo Ufumu Wosatha”*** (Danieli 7:27); mphotho yawo kotero, ndiyo moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu womwe udzakhazikitsidwe pa dziko lapansi lino; lomwe ndi panso pa thambo la Kumwamba.

4.8 UDINDO WATHU PAMASO PA MULUNGU YEHOVA

Ngati munthu ali ndi “*Mzimu*” limene timanena kuti ndi gawo limodzi la thupi ndi uthunthu wake lomwe silikufa, ndipo kuti munthu akafa mzimuwo umapita kumoyo wosatha kumalo kwina kwake, komanso kuti umapitanso ku malo a mazunzo ngati munthuyo adaachimwa; tiona kotero kuti zonsezi zikuonetsa kuti mwa apo ndi apo, anthu amadziwa kuti ali ndi udindo pamaso pa Mulungu. Taonetsa kale zoona zeni zeni za uthunthu wa munthu kuti ndi ofanana ndi nyama ndipo kuti mwaichi, mzimu wa munthu sikanthu kosafa kamene kamapezeka mthupi la munthuyo monga ena amanenera. Tidziwe kuti ngakhale anthu enawo amanena kapena kukhulupirira motere, ena mwa anthu okhulupirira adzalandira moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu. Tikudziwanso kuti sionse omwe anakhala padziko lapansi amene adzaukitsidwe; monga nyama, munthu amakhala ndi moyo naafanso, kuwola ndinso kubwerera kunthaka. Popeza padzakhala chiweruzo, chimene chidzagamule milandu ya anthu ena kuti adzapite ku moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu ndi anthu ena kuimfa chigonere, tiyenera titsimikizirane pano kuti sionse anthu amene adzaweruzidwe ayi. Okhawo amene akuzindikira za Mulungu ndipo adzaukitsidwa kwa akufa, ndi omwe adzaweruzidwe ndi kulandira mphoto zawo.

Kuti munthu adzafike poweruzidwa, ndiye kuti pali malamulo omwe anakhazikidwa ndipo kutinso iye akuwadziwa. Ngati sakuwadziwa malamulo otere, pamakhala pobvuta kuti azindikire chimene iye walakwa. Kotero, ndiudindo wa munthu’yo kumvera malamulo okhazikitsidwawo ngati iye akuwadziwadi. Ngati saamamvera malamulo’wo, iye amaweruzidwa pabwalo lomwensu amalidziwa. Izi zimakhalira kwa munthu’yo kupitanso kumalo a chiweruzo kuti akaweruzidwe chifukwa iye amadziwakonso kubwaloko. Ife malamulo athu ndiwo Mau a Mulungu ndipo chiweruzo chathu, chiyenera kudzagwirizana ndi chiyembekezo chathu pa Mau’wo maka maka ngati tachita bwino kapena ayi. Izinso zikhudza kwambiri onse omwe akudziwa ndi

kuzindikira chikonzero chimenechi kudzera m'Mau a Yehova. Khristu anafotokoza motere: **“...Iye amene akana Ine, ndi kusalabadira mau anga, aliyense womuweruza iye; mau amene ndalankhula, iwowa adzamuweruza tsiku lomaliza”** (Yohane 12:47,48). Choncho, iwo amene sanadziwe kapena kuzindikira Mau a Khristu, ndipo sadakhalenso ndi mwayi wina ulionse womukana kapena kumulandira Iye, saali ndi udindo wina ulionse oweruzidwa patsiku la chiweruzo'lo. **“...Pakuti onse amene anachimwa opanda lamulo adzawonongeka opanda lamulo; ndi onse amene anachimwa podziwa lamulo adzaweruzidwa ndi lamulo;”** (Aroma 2:12). Mwaichi, onse amene sanadziwe chikonzero ndi zofunikira za Mulungu, adzatha, naafa monga nyama zimafa osadziwa komanso osazindikira zimenezi m'chimbuzi mbuzi, komanso osawona chiweruzo; Pamene ena onse amene amaswa malamulo a Mulungu, ayenera kudzaweruzidwa m'kuzindikira kwawo kwa malamulo kotero, ngati afa asanaweruzidwe, adzaukitsidwa kuti aweruzidwe molingana ndi nzeru zawo pa mbali ya malamulo a Mulungu.

Pamaso pa Mulungu, **“tchimo siliwerengedwa** (kuwumirizidwa) **popanda lamulo”**; **“tchimo ndi kusaweruzidwa”** (Aroma 5:13; 1 Yohane 3:4; Aroma 3:20). Munthu chomwecho, sadzawumirizidwa kupita kuchiweruzo popanda kuzindikira malamulo a Yehova monga tawerenga m'Mau ake, **“tchimo silidzawumirizidwa kwa munthu”**, choncho, munthu osadziwayo, sadzawukitsidwa ndipo sadzaweruzidwa chifukwa kutero, nkumuwumiriza kuchita zinthu zimene iye sakuzidziwa. Moteronso, onse amene anafa ndipo sanadziwe kanthu, naalephera kuzindikira Mau a Mulungu, kapena tinene kuti sanakhalepo ndi mwayi umenewu ngati momwe ziliri nyama zimene sizidziwa chirichonse pa chikonzero cha Mulungu popeza Mau'wo ankalalikidwa kutali ndi iwo, sadzawukitsidwa ndipo kuti adzakhalabe chifere monga momwe nyama ndi zomera zakufa zonse zimakhallira lero, komanso momwe zidzakhalire panthawiyo popeza iwo lerolino ali chifere osadziwa chimene chikuchitika. Anthu otere adzakhalabe akufa m'chimbuzi mbuzi chawo. **“...munthu... wosadziwa, afanana ndi nyama zakuthengo zomwense zimafa”** (Masalmo 49:20). **“Ayikidwa m'manda ngati nkhosa** (zimene sizimadziwa chirichonse[Masalmo 49:14])”.

Ife timakhala ndi udindo kwa Mulungu pokha pokhapo tikadziwa mwachimvekere, zofuna ndi njira za Yehova; Kotero, timachita zonse monga Iye afuna ife tichite ndipo izi, ndi zimene zimatiyenera ife kuti tidzawukitsidwe ngati anthu a udindo ndi kuonekera pamaso pa Khristu Yesu, kuti tikaweruzidwe pamene Iye adzakhale pa Chimpando wa Chimfumu Wake. Tidziwensho kuti sioyera mtima okha kapena obatizidwa okha amene ali ndi udindo kwa Mulungu popeza anamudziwa Iye naadziwanso zomwe Mulungu Yehovayo amafuna iwo achite nthawi zonse ayi, yense amene anamvapo za Mulungu naona kufunikira kochita chifuniro chakecho alinso ndi udindo umenewu. Munthu ayenera kukhala ndinso kuchita zoyenera monga Mulungu amafunira kuti iye achite m'moyo uno Khristu asanabwere. Iyi ndi mfundo imene imabwerezedwa bwerezedwa m'Baibulo:-

- Yohane 15:22 akuonetsa kuti kudziwa Mau a Mulungu kumabweretsa udindo kwa munthu wodziwayo: ***“...ndikanapanda kubwera (Yesu) ndi kulankhula nawo sakadakhala nalo tchimo; koma tsopano alibe chowiringula pa machimo awo”***.
- Aroma 1:20-21 akunenanso kuti podziwa Mulungu, anthu sangathenso ***“kuwiringula”*** ndipo alibe chifukwa chonamizira. ***“...Kulibe m'modzi akhoza kudza kwa Ine (Yesu) koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza chalembedwa mwa aneneri, Ndipo adzakhala onse ophunzitsidwa ndi Mulungu. Yense amene adamva kwa Atate, naphunzira adza kwa Ine.”*** (Yohane 6:44,45).
- Mulungu ***“analekerera”*** ntchito za iwo amenedi sanamvepo Mau ake ndipo samadziwadi zofuna zake. Kwa iwo amene amadziwa njira ndi zofuna zakezo, amawaonetsetsa nawazindikira kotero, amayembekezera kuti iwo achita zabwino nthawi zonse mogwirizana ndi zofuna zake zija zomwe iwo amazidziwanso (Machitidwe 17:30).
- ***“Ndipo kapolo uyo odziwa chifuniro cha Ambuye wake, ndipo sanakonza, ndi kusachita zonga za chifuniro chakecho,***

adzakwapulidwa mikwapulo yambiri. Koma iye amene sanadziwa, ndipo anazichita zoyenera mikwapulo, adzakwapulidwa pang'ono (mwachitsanzo, adzangokhala chifere osalawanso kukoma kapena kuyipa kwa moyo wa nthawiyo owukitsidwa kwa akufa). *Ndipo kwa munthu aliyense adampatsa zambiri, kwaiye adzafuna zambiri; ndipo amene anamuyikizira* (kuwonjezera) *zambiri, adzamuuzza abwezere zoposa*” (Luka 12:47-48) – Nanga kweni kweni Mulungu adzatani kwaife anthu?

- *“...Potero, kwaiye amene adziwa kuchita bwino, ndipo sachita bwino, kwaiye kuli tchimo*” (Yakobo 4:17).
- Udindo wapadera wa ana a Israeli kwa Mulungu, udaagona pa zimene Yehova anawauza zokhudza Iye (Amosi 3:2).
- Chifukwa cha chiphunzitso ndi mfundo imeneyi ya udindo wathu kwa Mulungu, *“...Pakuti pakadakhala bwino kwa iwo* (amene adabwerera m'mbuyo) *akadakhala osazindikira njira ya chilungamo, ndi* (kuti ngakhale) *poyizindikira, kubwerera kutaya lamulo lopatsidwa kwa iwo*” (2 Petro 2:21). Ndime zina powonjezera mfundo imeneyi ndi izi:- Yohane 9:41; 3:19; 1 Timoteo 1:13; Hoseya 4:14; Deuteronomo 1:39.

Kizindikira kuti Mulungu alipo ndinso kudziwa zofuna ndi cholinga chake, ndi zomwe zitiyenezadi ife kukaonekera pamaso pa Khristu Yesu ndinso kuyandikira pafupi ndi Chimpano Chake cha Ufumu; Mwaichi, onse amene sanamve Mau a Mulungu, afanana ndi nyama zomwe ziribenso udindo wina uliwonse pamaso pa Mulungu Yehova popeza izo *“sizimadziwa chirichonse ndipo zonse zimafa m'chimbuzi mbuzi*” (Masalmo 49:20). Pali chitsimikizo chokwanira chimene chikuonetseratu kuti sionse amene anali ndi moyo ati adzawukitsidwe patsiku lomaliza ayi:-

- Anthu akale a dziko la Babelo *“sadzaukitsidwa kwa akufa*” chifukwa sanadziwe zambiri zokhudza Mulungu wamoyo wa choonadi wa Israeli (Yeremiya 51:39; Yesaya 43:17).

- Yesaya podzilimbikitsa iye mwini ananena: *“Yehova Mulungu wathu (wa ana a Israeli), pamodzi ndi Inu Ambuye ena adatilamulira ife (ena monga Afilisiti ndi anthu a ku Babulo) ...Koma mwa Inu nokha tidzatchula dzina lanu. Iwo afa, atha sadzauka; chifukwa cha inu munawazonda, ndi kuwaononga, mwathetsa chikumbukiro chawo chonse,”* (Yesaya 26:13,14). Onani kuti mwachimvekere iwo sadzaukitsidwanso: *“sadzaukanso, ...sadzakhalanso ndi moyo ... chikumbukiro chawo chinatha”*. Ana a Israeli ndi osiyana ndi mitundu ina iriyonse popeza iwo anadziwa kale za mbiri ya Mulungu pokhudza kuukanso kwa akufa chifukwa anaphunzira kale kudziwa zoonadi zeni zeni za Mulungu wao:- *“Akufa anu (ana a Israeli) adzaukanso ndi moyo, pamodzi ndi thupi langa, iwo adzaukanso kwa akufa”* (Yesaya 26:19).
- Tikamalankhula zambiri za anthu a Mulungu, a Israeli, timamva kuti patsiku lobwera Khristu, *“...ambiri a iwo ogona m'mfumbi lapansi adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi 'm'nyozo?' wosatha”* (Danieli 12:2). Kotero, *“ambiri”* osati onse, mwa a Yuda adzaukitsidwa, chifukwa iwo ali ndi udindo pamaso pa Mulungu monga alinso osankhidwa. Ena onse amene sakudziwa kapena sanadziwe china chirichonse chokhudza Mulungu *“adzagona chigonere, ndipo sadzaukitsidwa ngakhale pang'ono,”* popeza sanatha kupeza *“Mau a Mulungu”* (Amosi 8:12,14).

TSOPANO TAPHUNZIRA KUTI:

- Kudziwa ndi kuzindikira Mau a Mulungu kumabweretsa udindo wathu kwaike tokha pamaso pa Yehova.*
- Okhawa amene ali ndi udindo (kapena tinene kuti amene anadziwa chikonzero cha Mulungu) ndi amene adzaukitsidwe ndinso kuweruzidwa ndi Khristu pamene Khristu'yo adzabweranso padziko lapansi lino.*

- iii. *Ena onse amene samadziwa zambiri zokhudza Mulungu wa choonadi kotero, adzagona chigonere monga nyama ndi zomera zimachitira zikafa.*

M'mene tawerengera pano, zikutanthauza kuti tiyenera kukhulupirira monga mwa malembo kuti anthu mazana mazana, kuchokera kale mpaka lero lino, amene sanathe kudziwa kapena kukhala ndi mwayi ozindikira Mulungu woonadi; Ndikuti sanathe kudziwa zambiri pa ulaliki wa Uthenga Wabwino, ena onse a matenda a ubongo amene sanathe kudziwa Mau a Mulungu a m'Baibulo; ana ang'ono ang'ono omwe anamwalira kale kale asanafike pa msinkhu wozindikira zinthu monga Uthenga Wabwino; onse amene'wa ali mgulu limeneri losadziwa ndinso kuzindikira choonadi cha Mulungu wamoyo ndikuti saali ndi udindo wina uliwonse pamaso pa Mulungu. Kotero, tidziwa kuti anthu amenewa monganso nyama ndi zomera zonse, sadzaukitsidwa kwa akufa ngakhale kale makolo awo anachita bwino pamaso pa Mulungu. Tikudziwa kuti chikonzero chotere, ndi chosiyana kwambiri ndi zilako lako ndinso zoganiza zathu; Komabe, tiona kuti kudzipereka, kudzichepetsa komanso kumvera kwathu mzinthu zooneka zonyozeka ngakhale ziri zofunikira ngati zimenezi, ndi zimene zimakonza tsogolo lathu labwino pamaso pa Yehova ndi Mwana Wake Yesu Khristu. Tidzadziwa choonadi cheni cheni chimene ife tikachipeze kwa Iye, ndipo tidzakhutira nacho popatsidwapo mphothoyo. Tikafatsa bwino bwino ndikuganizira moyenera pa nkhani iri pamwambayi, imene tawerenga kale kuchokera m'Baibulo, tidzaona kuti ndi zomveka bwino maka maka tikamawerenga mozama, molakalaka kudziwa Mau a Yehova a chiyero'wa omwe ndi opindulitsa.

Tikafika apa, sindikhulupirira kuti palinso wina amene angakayikire njira yoona yeni yeni ya Mulungu pa mfundo zimene tawonazi: *“Koma munthu iwe, ndiwe yani wakubwezera (wotsutsa) Mulungu mau? Kodi chinthu chopangidwa chidzanena ndi amene anachipanga, Undipangirani ine chotero?* (Aroma 9:20). Mwina nthawi zina sitimamvetsa bwino komabe sitiyenera ndiponso sizingatheke kuti tiwiringule pamaso pa Mulungu kuti Iye ali wolakwa, wokondera ndi wosalungama. Mulungu ndiye wachilungamo, Atate wachikondi ndinso wachiyero. Iye ndi wamphamvu ndi wachifundo chochuluka. Imfa ya mwana wa Davide ikhoza kutipatsa chitsanzo chokwanira pa mutu umenewu: 2

Samueli 12:15-24 akutifotokozerwa momwe Davide adapempherera mwamphamvu kotero, mwana wake akhale ndi moyo koma pomaliza anabvomereza kuti cholinga cha Mulungu pamwana wake chiyenera kukwaniritsidwa: ***“Pamene mwanayo akali ndi moyo, ndinasala kudya ndi kulira, pakuti ndinati, Adziwa ndani kapena Yehova adzandichitira chifundo kuti mwanayo akhale moyo. Koma tsopano wafa, ndidzasaliranjinso kudya? Kodi ndikhoza kumbweza? Ine ndidzamuka kuli iye, koma iye sadzabweranso kwaine”*** Ndipo kenaka Davide anasangalatsa Beteseba, nalowa mwaiye, nakhala ndi mwana winanso.

Mwina ena angaganize kuti kuli bwino osapitirizanso kuphunzira Mau a Mulungu kotero, sangakhalenso ndi udindo wina uliwonse umene ungawadziwitse chimene iwo ayenera kuchita pomvera Mulungu ndinso kuti asadzaweruzidwe. Popeza anthu otere adziwa kale mphamvu ya Mulungu, kuti iwo amasungidwa komanso kuti amasamalidwa ndi Iye ngakhale Yehovayo sakumudziwa. Tiyenera kudziwa ife tonse timatetezedwa ndi Mulungu wathu. Iwo amene angaganize izi ayenera kudziwa kuti mphamvu ya Mulungu yagwira ntchito yaikulu m'miyoyo yawo. M'njira imeneyi, iwo anazindikira kale kuti Mulunguyo ndiye chikondi chimene amachidziwacho koteronso, ***“...sanalole kuti ife titayike ...”*** ndipo ***“anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye, asatayike koma akhale nawo moyo wosatha”*** (1 Akorinto 4:8; 2 Petro 3:9; Yohane 3:16). Mulungu apa, waonetseratu kuti amafunitsitsa ife tikalowe ndinso kuti tikakhale mu Ufumu Wake. Ichi ndi chimene anatilengera.

Ulemu ndi zonse zabwino ngati zimenezi ndi zimene zimabweretsa udindo kwaife pakati pathu ndi Mulungu. Tiona kuti chikonzero chotere sicholempera kwaife tikachisenza patokha ayi; ngati timamukonda Mulungu m'choonadi, tidzabvomereza kuti lonjezo lake la chipulumutso silidzakwaniritsidwa kwa aliyense ayi, koma kwa okhawo ochita chifuniro chake m'choonadi. Mwaichi, Yehova adzatipatsa mphotho yake ya moyo wosatha wachisangalalo chifukwa cha kukhutsidwa kwathu pochita chifuniro chake cha chiyeo.

Monga tsopano tonse timakhutira pakumva mayitanidwe a Mau a Mulungu, tidzazindikira kuti ngakhale tiyende pakati pa chikhamu cha anthu ochita zoyipa, Mulungu akutionetsa ndi chidwi pa zochita zathu ngati zikuloseradi ku

chikonzero ndi chikondi chake chomwe taphunziracho. Diso lake la chikondi chosatha ndi dzanja lake la mphamvu, zimakhala paife pamene tasenza udindo womudziwa Iye ngati Mulungu Yehova wa choonadi pakati pathu. Kotero, tiyenera kukondwera pokhala kupfupi ndi Chiuta nthawi zonse ndipo kuti Iye amatisunga ndi kutiyang'anira nthawi zonse. Tilakelake kudziwa zambiri za Yehova moteronso, tizikhala m'chiyero ndi choonadi ngati momwe Iye amakhala ndipo tikhala ana ake.

4.9 HELO (MANDA KAPENA KUTI DZENJE)

Malingana ndi m'mene anthu amadziwira za liwu loti "Hell", amanena kuti ndi kumalo komwe "mizimu yosafa imene imapezeka mkati mwamatupi a anthu" imafikirako munthuyo akamwalira, kapenanso kuti ndikumalo amazunzo kwa iwo amene adzakanidwe ndi Khristu likadzafika tsiku la chiweruzo. Ife tikukhulupirira kuti Baibulo limatiphunzitsa kuti liwu loti "Hell" tanthawuzo lake ndilo "manda" kapena kuti "dzenje la manda" komwe munthu wakufa amakwiridwa.

M'chi Hebri ndi m'chi Greek, liwu loti "Hell" ndi "Sheol" limatanthauza kuti "malo ofotseredwa" kapena tinenenso kuti "malo ophimbidwa". Liwu loti "Helo" ndi liwu lomwe silidamasuliridwe m'chilankhulo china chirichonse chifukwa kunali kobvuta kutero, ndipo kumaliza kwake kwa liwu limeneri m'Chizungu ndiko kuti "*Hell-met*" kutanthauza kuti "*kuphimba mutu*", mwachitsanzo, chipewa; "*kukwirira*" kapena "*kubisa pofundika thunthu la munthu*". Choncho, liwu loti "*Helo*" kapena "Hell" tingatanthauzire kuti ndi "*manda*" m'Chichewa. M'Baibulo, malo amenewa ophimbidwa, omwe m'Bulu Lopatulika ndi "Hell" kapenanso kuti "Hade" ndi "Manda" m'Chichewa. Pali malo ambiri m'Baibulo omwe akutanthauzira mau oti "sheol", "Hade", "Hell" kuti ndiwo "Manda" monga Baibulo loyamba lidalembedwera. Motero,

sizingatheke kuti mau amenewa a “Hell” angaimire kapena tinene kuti angatanthauzidwe kuti ndi malo ena a mazunzo kumwamba ayi chifukwa m’Baibulo liwuli, latanthauzidwa kale momveka bwino kuti ndi malo okwiriramo anthu akufa, manda. Werengani zitsanzo zotsatirazi kuti mudzionere nokha matanthauzo’wa:-

- i. **“...Oyipa achite manyazi, atonthole m’manda** (sheol [Masalmo 39:17]) – mwachitsanzo, kunena kuti sadzalira ndi ululu ali m’manda.
- ii. **“...Koma Mulungu adzawombola moyo wanga kumphamvu ya manda”** (sheol [Masalmo 49:15]) – Apa tiona kuti uthunthu wa Davide unayenera kuukitsidwa kwa akufa kuchokera m’dzenje la manda.

Chikhulupiriro chakuti “Hell” ndi malo a chilango cha anthu ochimwa kumwamba, sichingakhale choona tikamaganizira matanthauzo a Mau tawerengawa ndinso kuti Mau amenewa akuchokera m’Baibulo limene ife timakhulupiriradi kuti ndiwo Mau a Mulungu. Tionanso kuti ngakhale ziri choncho, iwo ndi amene adzaukitsidwe kwa akufawo (kuchokera ku manda). Hoseya 13:14 akutitsimikizira nkhani imeneyi motere: **“..Ndidzawaombola** (anthu a Mulungu) **kumphamvu ya ku manda** (sheol), **ndidzawaombola kuimfa; imfa, miliri yako iri...**” Mau omwe’wa ananenedwanso m’buku la 1 Akorinto 15:55 ndipo akutsimikiziranso kuukanso kwa akhristu kwa akufa pamene Khristu Yesu adzabweranso panso pano. Tikaonanso masomphenya a m’Phunziro 5.5, **“imfa ndi Hade** (manda) **zinapereka akufawo anali m’menemo”** (Chibvumbulutso 20:13) Onaninsu kuti imfa, mwachitsanzo, manda kapena tinene kuti “Hade” zonse zikufananizidwa ngati chinthu chimodzi ndipo izi ziri choncho tikawerenga m’Bulu la Masalmo pa 6:5.

Mau a Hana pa 1 Samueli 2:6 akuonetseratu poyera tanthauzo leni leni la imfa ndi “Hade” **“..Yehova amapha, napatsa moyo; Iye amatsitsa** (amatengera munthu kumanda) **kumanda”** (Hade, sheol, Hell etc) **nawukitsanso.”**

Monga taona kuti “Hade” zonse tanthauzo lake ndi kuti “Manda”, ndiye kuti oyerera mtima onse adzapulumutsidwa kuzonsezi poukitsidwa komanso kupatsidwa moyo wosatha. Kotero, zikhoza kutheka kwa munthu kufa ndi kulowa m’manda (Hade, Hell kapena tinene kuti Sheol), koma komaliza kwake ndiko kuukitsidwa kwa akufawo. Chitsanzo china chachikulu m’njira yomweyi ndicho chakuti Yesu Khristu amene **“sanasiyidwa m’Hade, ndipo thupi lake silinaona chibvundi”** (Machitidwe : 2:31) popezadi kuti Yesu Khristu’yo anaokitsidwa kwa akufa. Onani kuti thupi la Yesu ndi Mzimu wa Yesu zonse zikulembedwa kuti ndizo chinthu chimodzi chomwe ndicho (uthunthu wake) chomwensu sichinaone chibvundi. Chokha chongoti thupi lake **“..silinasiyidwa m’Hade”** zikuonetseratu kuti thunthu la Yesu Khristu atafa linakhala m’manda kwakanthawi, mwachitsanzo, masiku atatu liri m’manda. Kungomva chabe kuti Yesu Khristu anapita ku Hade (Manda), zikutitsimikizira kuti simalo opitako ochimwa okha okha ayi, koma kuti anthu onse akafa, amapita kumalo amenewa omwe ndi “Manda”.

Onse ochimwa ndi olungama amapita kumanda, ku Hade kapena tinene kuti ku “Hell” mwachitsanzo, amakayikidwa kudzenje akafa. Choncho, Yesu, **“anayika manda ake pamodzi ndi oyipa”** (Yesaya 53:9). Mofanana ndi mau amenewa, zitsanzo zina za anthu olungama amene amapita ku Hade ziripo zambiri. Yakobo ananena kuti **“..Pakuti ndidzatsikira kumanda** (Hell, Hade kapena Sheol) **kwa mwana wanga, ndirinkulirabe”** (Genesis 37:35). Yakobo adanena mau amenewa pamene ankalirira mwana wake Yosefe yemwe anagulitsidwa kwa ogula akapolo.

Mulungu anakonza kale ndondomeko yoyenera ya chilango ngati munthu atapezeka kuti wachimwira Mulungu moterodi, “mphotho ya uchimo ndiyo imfa (Aroma 6:23; 8:13; Yakobo 1:15). Tinaonetsa poyambirira kuti munthu akafa chotsatira chake ndicho kusadziwa chochitika china chirichonse ndi kuyiwala zonse zidachitika iye akadali ndi moyo. Tchimo limabweretsa chionongeko cha moyo wa munthu osati kuzunzika kosalekeza ku malo otchedwa “Hade”, “Hell” kapena “Sheol” ayi (Mateyu 21:41; 22:7; Yakobo 4:12), monga anthu onse anaonongedwa ndi kusefukira kwa madzi (Luka 17:27,29), komanso ana a Israeli anafa m’chipululu chifukwa cha machimo awo (1 Akorinto 10:10). Tiona kuti m’malo onsewa, anthu ochimwa onse anafa popeza anachimwa pamaso pa

Mulungu Yehova wao osati chifukwa chakuti anaponyedwa m'dzenje la mazunzo mpaka muyaya ayi. Tadziwanso kotero, kuti oyipa ndi ochimwa onse sadzalangidwa kumva kuwawa kwa muyaya, kosatha ayi; Koma kuti adzafa, nadzakhala chigonere osadziwa chochitika, pamene anzawo adzakhala akusangalala ndi Ambuye Wathu Yesu Khristu mpaka muyaya.

Taphunziranso kuti Mulungu samatiwerenga ife pamodzi kukhala mgulu la ochimwa lodzaukanso kwa akufa ngati tidachimwa komanso ngati ifeyo panthawi yochimwayo, tinali tisanamvepo Mau a Mulungu Yehova Wathu. Mwachitsanzo, ngati tinkachita izi mkusazindikira kwina kulikonse, komanso posadziwa chilamulo chirichonse. Munthu amene saadziwa lamulo sangachimwire wina ali yense (Aroma 5:13). Onse amene anafa osadziwa Mau a Mulungu kotero, adzakhala chigonere osadziwa chochitika pakati pawo ndi kunja kwa iwo, ndipo sadzalangidwa chifukwa lamulo kwa iwo liribe gawo. Iwo amene anamva Mau a Chiuta, nadziwa zolinga ndi zofunikira pa chipulumutso chawo ndi Mulungu, adzawukitsidwa, naaweruzidwa pamene Khristu Yesu adzabweranso padziko lapansi lino. Ngati adzapezeke kuti anachimwa pamaso pa Mulungu pamene iye adaali moyo padziko lapansi lino, adzalangidwa m'chilango cha imfa, nakhala chifere mpaka m'nthawi zosatha popeza tonse tidziwa kuti mphotho ya tchimo ndiyo imfa. Iyi idzakhala "imfa ya chiwiri" kwa iwo ndipo imfa yake idzakhala yopwetekadi chifukwa adzasilira anzawo akupatsidwa moyo wosatha pamaso pawo, ngati momwe timawerengera pa Chibvumbulutso 2:11; 20:6. Anthu amenewa adzawukitsidwa nakhalanso ndi moyo, nalandira chiweruzo; ndipo kenaka adzafa kachiwiri koma komaliza, nakhala chikhalire akufabe osadziwa chochitika kudziko mpaka muyaya wa muyaya.

M'njira imeneyi, chilangocho chidzakhala chosatha popeza adzakhala chifere mpaka muyaya osaukitsidwanso. Munthu kukhala chifere mpaka muyaya pamene anzako awukitsidwa kumoyo wosatha, ndi chilango chowawa komanso chosatha! Chitsanzo china chimene chikuonetsa mafotokozedwe a mtundu ngati umenewu, ndi Deuteronomo 11:4. Ndime imeneyi ikukamba za a nkhondo a mfumu Farao kuti "*..anawonongedwa mpaka lero lino.*" Kuonongedwa kwa a nkhondo kunachitika kale ndipo kunatha kale lomwelo; ngakhale m'Baibulo tikuwerengabe kuti anawonongedwa mpaka lero lino. Izi choncho,

sizikutanthauza kuti a nkhondowo akuonongedwabe mpaka lero lino ayi, tiona kuti a nkhondo a mfumu Farao sanabvutitsenso kapena tinene kuti sakubvutitsabe ana a Israeli mpaka lero ayi kotero, sangakhale kuti Mulungu akuonongabe a nkhondowo mpaka lero lino ayi; Moteronso, “*..Yehova anawononga kufikira lero*”. ‘Anawaononga kufikira lero’ kukutanthawuza kuti mpaka lero Mulungu atawaononga anthu ankhondo aja, sanawabvutitsenso ana a Israeli chifukwa ankhondowo anafa.

Ngakhale okhulupirira anzathu kalelo m’Chipangano Chakale, ankadziwa kuti kudzakhala kuukitsidwa kwa akufa pa tsiku lomaliza pamene Khristu adzawonekera, ndipo kuti ochimwa onse mkuzindikira Mau a Mulungu (ochimwa mwadala), adzaweruzidwa kuimfa ya muyaya, naabwerera ku manda. Buku Lopatulika pa Yobu 21:30,32 tikuwerenga motere: “*..munthu woyipa..Potsiriza pake adzapita naye ku manda, ...naadzadikira pamanda pake mpaka muyaya...*” Limodzi mwa mafanizo a kubweranso kwa Yesu Khristu posimba za chiweruzo cha anthu oyipa padziko, akunena kuti “*adzawakantha*” pamaso pake (Luka 19:27). Izi sizingagwirizane ndi chiphunzitsa chonena kuti anthu ochimwa akafa, amaponyedwa mng’anjo ya moto wosazima wosatha ku “Hade”. Apa tionanso kuti Mulungu sangakhale wachifundo ngati angatilenge kenaka n’kutilanga m’moto wosatha chifukwa cha machimo omwe tinachita mzaka 70 zokha ayi. Mulungu kotero, sangasangalatsidwe ndi chilango cha munthu wotere; popeza Iye anawona ndipo anakonza kale chilongosoko cha moyo wosatha ngati tichita bwino, ndinso imfa ngati mphotho ya uchimo chifukwa Iye amadana ndi tchimo. Mulungu Yehova choncho, sadzalanga ndi chilango chomamva kuwawa kosalekeza cha moto mpaka muyaya monga ena amanenera ayi (Ezekieli 18:23,32; 33:11 cp. 2 Petro 3:9).

Akhristu ambiri samatha kusiyantsa pakati pa Mau oti “Hell”, Hade ndi moto malingana ndi matanthauzidwe awo a mau amenewa ndipo ena mwa iwo amati ndinjira ya chilango cha munthu. Izi zikusiyana ndi m’mene Baibulo limanenera za nkhani imeneyi kuti “Hell” ndi “Manda”. “*..Ayikidwa m’manda* (hell, hade, ndi sheol etc) *ngati nkhusa; adzadyedwa ndi imfa*” (Masalmo 49:14) – zomwe zikutanthauziradi kuti ku manda ndi malo a cheete, kulibe phokoso lina lililonse ayi. N’chifukwa chake, ngakhale thupi la Khristu linakhala masiku atatu

m'manda (Hade, Hell) ndipo “*..silinaona chibvundi*” (Machitidwe 2:31). Izi sizikanatheka kukanakhala kuti Hade (Hell) ndi malo komwe kuli moto wosatha wamuyaya ayi. Ezekieli 32:26-30 akutipatsa chithunzi thunzi chakuti anthu onse a mmayiko momwe mudali a nkondo a mphamvu lero, kuti onsewa ali chigonere m'manda (Hade, Hell kapenanso tinene kuti Sheol) – mphamvu zawo zonse zija zidayiwalika, palibenso amene angawakumbukire, komanso kuti iwo paokha sakukumbukira zomwe akhala akuchita: “*...amphamvu osadulidwa adagwawo amene anatsikira kumanda* (Hade, Hell, Sheol) *ndi zida zawo za nkondo, amene anawatsamiritsa malupanga awo pamitu yawo; ...anagona osadulidwa pamodzi ndi iwo otsikira kudzenje...*” Ndime zimenezi zikunena za chikhalidwe chodziwika cha anthu amene amakwirira mitembo ya anthu omwalira pamodzi ndi zida zawo, ndinso kutsamiritsa mitu ya mitemboyo pa zida zawozo, zimene anthuwo ankagwiritsa ntchito akadali ndi moyo. Zonsezi zikutifotokozera za munthu yemwe wangofa ndipo pali chikonzero chakuti munthu wakufayo akamutaye ku manda (m'dzenje) pamodzi ndi zida zake zomwe amagwiritsa ntchito ku nkondo, zimensenso zimayikidwa mu “Hade” (kapena tinene kuti mu Hell) pamodzi ndi iye. Anthu otere atakhala ndi mwayi wofotokoza zomwe iwo akumana nazo komanso zomwe zimachitika ku Hade'ko, sangabvomereze zabodza zambiri zimene alaliki ena amalalikira lero kuti ndithu “Hell / Hade” ndi malo omwe kuli moto wosatha ndichilango chosathanso ayi. Zinthu zooneka ndi maso athu monga zida zankondo zomwe zimayikidwanso m'manda pamodzi ndi mwini zidayo, zonse zikukambidwazi, pano zikuonetseratu poyera kuti Baibulo limanena za “Hade” ngati malo okwirirako anthu akufa (ngakhale nyama ndi zinthu zina zonyasa); osati mizimu monga ena amanenera kuti ndi komwe kuli mazunzo osatha ayi. Iye ndi zinthu zathu (monga ngati zida zonse), timathera kumeneku (m'manda). Kotero, n'chifukwa chake Petro ananena, “*Ndalama yako itayike nawe*”, (Machitidwe 8:20).

Tionanso kuti ngakhale zomwe anawona Yona zikusiyana koposa ndi malalikidwe a masiku ano pokhudza nsonga imeneyi ya “Hade” kapena “Hell”. Iye atamezedwa wamoyo ndi nsomba ija, “*...Yona anapemphera kwa Yehova Mulungu wake ali m'mimba mwa nsombayo. Ndipo 'Ndinaitana Yehova m'nsautso yanga, Ndipo anandiyankha ine; Ndinapfuula ndiri m'mimba ya manda'* (Hade, Hell)” (Yona 2:1,2). Apa zikugwirizana ndithu “manda a

m'mimba" ya nsomba ija ndinso mimba ya manda eni eni popeza zonsezi ndi malo okwiriridwa, ophimbidwa.

Mau oti "Hade, Hell" kapena "Sheol" onse amatanthauzira kuti "malo ophimbidwa, okwiriridwa", monga momwe mimba ya nsomba ija inakwirira Yona atamezedwa. Pano sitinganene kuti mimba ya nsomba ija ikhale kumwamba popeza yatchulidwa kuti ndi "manda" (Hade, Hell, Sheol) ayi. Tionanso kuti nsombayo inamusanza Yona uja kuchokera m'manda a mimba yakeyo (omwe ndi malo amene anamukwirira Yona uja), zomwedi zikulosera ndinso kuyimira kuukitsidwa kwa akufa kwa Yesu Khristu kuchokera m'dzenje la manda (onani Mateyu 12:40).

CHIPHIPHIRITSO CHA MOTO

Baibulo limagwiritsa ntchito mau ophiphiritsa monga "moto wosazima ndi wosatha" pofuna kufotokozera mkwiyo wa Mulungu pa tchimo la munthu. Tchimo ndi limene Yehova amadana nalo ndipo anakonza kale kuti mphotho yake ndi imfa yomwe ndiyo kugona chigonere kosalekeza, kugonadi m'manda mpaka muyaya. Anthu a mu mzinda wa Sodoma analangidwa ndi "moto" wosatha, wamuyaya (Yuda 5-7) mwachitsanzo, anaonongedwa kwathunthu chifukwa cha zoyipa za anthu okhala mu mzindawu. Lero lino, mzinda wa Sodoma kulibe popeza unaphwasulidwa koma malo ake ndiwo amene alipo omwedi tsopano ndi panso pa Nyanja ya Mchere (Dead Sea); Malo amenewa mutapitako lero, mukawona nokha kuti kulibe moto ngakhale kuti tawerenga za "moto wosatha" pa Yuda 5-7. Chimodzi modzinso anthu okhala mu Mzinda wa Yerusalemu anachenjezedwanso kuti adzalandidwa ndi "moto wosatha" wa mkwiyo wa Mulungu chifukwa cha machimo a ana a Israeli: **"...Koma simudzamvera Ine kulipata tsiku la Sabata, kusanyamula katundu ndi kulowa pa zipata za Yerusalemu tsiku la Sabata; pamenepo ndidzayatsa moto mzipata zakezo, ndipo udzatha zinyumba za Yerusalemu, osazimidwanso,"** (Yeremiya 17:27).

Yerusalemu ngati likulu la Ufumu wa Mulungu lomwe linaloseredwa ndi Mulungu yemweyo (Yesaya 2:2-4; Masalmo 48:2), Iye Yehova Mwini zonse sangalole kuti ife tiwerenge zimenezi ngati zeni zeni monga tikuoneramu,

kotero, kuti tiyembekezeredi kuti Mzinda wa Yerusalemu udawonongekadi kosatha mpaka lero ayi, sizoon. Ife tikudziwa kuti Yerusalemu akadalipo mpaka lero lino ndipo kuti Yehova Mulungu, ananena ichi m'chiphiphiritso osati ngati kuti zinalidi zoyenera kuchitika mwa zeni zeni ayi. Nyumba za mu Mzinda wa Yerusalemu zinawonongekadi koma osati ndi moto wosatha monga tawerenga ayi. Motowo ukanakhala kuti unaali wosatha ukanakhalabe ukuyakabe mpaka lero lino koma tiona kuti moto umenewu lero kulibe (2 Mafumu 25:9), komanso chodziwika china ndicho chakuti moto umenewu sudaali wosathadi ayi chifukwa udaatha nthawi yomweyo nyumba zija zitatha kupysa!

Mulungu momwemonso, analanga dziko la Edoma ndi moto womwe *“sudzazimikai usiku, ngakhale usana; utsi wake udzakwera nthawi zonse; m'mibadwo mibadwo lidzakhala labwinja...ndipo kadzidzi ndi nkhangubwi adzakhala m'menemo, ...Ndipo minga idzamera m'nyumba zake zazikulu”* (Yesaya 34:9-15). Pona kuti nyama ndi zomera zidzakhale ziripo m'mabwinja owonongekawo, liwu loti “moto wosatha” pano liyenera kutanthauzidwa mwamtundu wina popeza tsopano tionadi kuti chidaali chiphiphiritso chabe cha zinthu zodzachitika kutsogoloko mu Mzinda wa Edoma. Tiona kuti mau amenewa a “moto wosatha” akutitsimikizira za “ukali wa Mulungu” pa tchimo la anthu a mu Mzinda wa Edoma kotero, “simoto wosatha” weni weni monga timaudziwira nthawi zonse ayi. Ichi chidaali chiphiphiritso chabe.

Mau oyambirira a m'chi Hebri ndi m'chi Greek omwe anamasuliridwa kuti “kosatha” m'Chingerezi, adayenera kutanthauzidwa kuti “nthawi ino” kapena kuti “nthawi yosadziwika” kapenanso “nthawi yomwe chinthu chidzathe kuchitika”. Ezekieli 32:14,15 ndi chimodzi mwa zitsanzo ngati zimenezi: *“..likhale lопасuka ndi la bwinja, dziko losowa zodzaza zake, pakukantha Ine onse okhala m'mwemo, pamene adzadziwa kuti Ine Ndine Yehova”* (Ezekieli 32:14,15 – onani kuti kumasulira kwake sikoyenera m'ndime imeneyi m'Chichewa Bible). Iyi ndinjira imodzi yodziwira tanthawuzo leni leni la mau oti “moto wosatha” m'ndime zimenezi.

Nthawi zambiri, Baibulo limakamba za mkwiyo wa Mulungu ngati kuti ndi “moto wosatha”: *“..Taonani mkwiyo wanga ndi ukali wanga udzathiridwa pa*

malo ano (Yerusalemu), *pa anthu ndi pa nyama...ndipo udzatentha osazima*" (Yeremaiya 7:20; Maliro 4:11 ndi 2 Mafumu 22:17).

Moto unakambidwanso mogwirizana ndi chiweruzo cha Mulungu pa tchimo, maka maka pamene Khristu adzabwerenso: "...*Pakuti taonani likudza tsiku lotentha ngati ng'anjo; akudzikuza ndi onse akuchita choyipa adzakhala ngati chiputu; ndi tsiku lirinkudza lidzawayatsa*" (Malaki 4:1). Chinthu chiri chonse chikatenthedwa, kapena thupi la munthu aliyense likawotchedwa ndi moto, limabwerera ku mpfumbi. Sizingatheke kuti thupi la munthu lizingowotchedwa mpaka muyaya osasandulika kukhala phulusa. Titsimikizira kotero, kuti "moto wosatha" umene ukukambidwa m'ndime zimenezi ndi ziphiphiritso za "mkwiyo wa Mulungu" chifukwa cha tchimo la munthu. Tinawerenganso kuti imfa ndi liwu loti "Hade" kapena "Hell" zalembedwa *kuti "ziponyedwa m'nyanja ya moto"* (Chibvumbulutso 20:14). Izi zikuonetseratu poyera kuti "Hade" kapenanso "Hell" sinyanja ya moto monga ena amanenera, ndipo kuti izi ndi zinthu ziwiri zosiyana m'matanthauzo tikitengera momwe Baibulo limafotokozera za mau amenewa. "Moto wosatha" kotero, m'ndime zimenezi ndi chiphiphiritso cha chionongo ndi "mkwiyo wa Mulungu" pa tchimo la munthu. Ndime yomweyi ikunenanso kuti manda adzawonongedwa chifukwa komaliza kwa chirumika choyamba mu ulamuliro wa Yesu Khristu, sikudzakhalanso imfa. Imfa ndi manda zonse zidzatha popeza tchimo lidzaonongedwa ndinso kugonjetsedwa m'chiweruzo cha Khristuyo!

GEHENA

M'chipangano Chatsopano pali mau awiri a m'chi Greek omwe anamasuliridwa mofanana ndi liwu loti "Hell". "Hell" ndiwo amodzi mwa mau amene amafanana m'matanthauzo ndi liwu la m'chi Hebri loti "Sheol" lomwense takambirana kale pamwambapa. "Gehena" ndi liwu lomwe linapatsidwa kapena tinene kuti kutchulidwa ku chimulu cha zinyalala zowuma ndi zina zowola, zimene zinkawunjikidwa ndinso kutayidwa kunja kwa Mzinda wa Yerusalemu. Malo otaya zinyalala otere akupezekanso m'mizinda yambiri ya mayiko okwera ndi ena okwera kumene lero lino padziko lonse lapansi. Chitsanzo cha malo otere ndi ku Manila m'dziko la Philippines komwense mungapezeko malo ena otayako zinyalala ngati zimenezi. Liwu loti "Gehena" silinamasuliridwe monga mau ena ngati "Hell" m'Chingerezi kapena chilankhulidwe china chirichonse

ayi, koma kuti linasiyidwa m'chilankhulo chake choyamba chomwe ndi chi Greek. Liwu lina lofanana m'matanthauzo ndi "Gehena" ndi la chi Hebri loti "Ge-ben-Hinnon". Malo amenewanso ali pafupi ndi Mzinda wa Yerusalemu (Yoswa 15:8), ndipo m'nthawi ya Khristu, unali mzinda wa zinyalala zambiri ndi zina zonyasa. "Gehena" kenaka, anadzasandulitsidwa kukhala malo otayako anthu akufa omwe anali zigawenga pamwamba pomatayapo zinyalala. Ndipo anthu amenewa, ankaponyedwa m'moto umene unkayaka nthawi zonse chifukwa cha zinyalala zambiri mbiri zomwe zinkakhala pa malo amenewa. Mwaichi, "Gehena" anakhaladi malo a chiphiphiritso cha chionongeko padziko lapansi.

Tionanso apa kuti matupi omwe ankaponyedwa pa motowo ankasanduka phulusa (kubwerera ku dothi). **"...Pakuti Mulungu wathu ndiye moto wonyeketsa"** (A Hebri 12:29); pa tsiku la chiweruzo; moto wa mkwiyo wa Mulungu Yehova pa tchimo la munthu, omwe udzanyeketse anthu onse ochimwawo, udzafikadi pa dziko lonse lapansi. Izi ndi zomwe tiyenera kuzindikira ndipo ziyenera kudziwika pakati pa a khristu onse; n'chifukwa chake kunalembedwa m'Malembo Oyera kuti ife tithe kupindula lero lino pamene tiwerenga mau okoma otere.

Tizindikirensa tsopano kuti pa chiweruzo chonse chimene chinachitika ndi Mulungu kwa ana a Israeli pamaso pa anthu a ku Babulo, "Gehena" adadzazidwa ndi mitembo ya anthu ochimwa pakati pa ana a Mulunguwo (Yeremiya : 7:32,33).

Yesu Khristu anakambapo mwa luso lake lochititsa chidwi za "Gehena", pophatikiza zonse zomwe zidalembedwa m'Chipangano Chakale ndi zomwense anthu ankadziwonera okha polumikiza zochitikazo ndi zimene ankazionazo kumalo komwe ankataya zinyalala kuja. Mwaichi, kunali ngati kuwatsimikizira anthu aja kuti onse omwe sadzaloledwa pa chiweruzocho adzatayidwa nadzaponyedwa m'Gehena (m'manda); Chomwe chidalidi chikumbutso chachikulu ndi phunziro lalikulu kwa anthu amene ankadzimvera Uthengawo pa nthawi ya Khristu'yo kuti ndithu, adzakanidwadi pamaso pa Khristu ngati alimbikira kuchimwa. Imfa kotero, idzawafikira iwo chifukwa cha tchimo lawo. Malo amenewa monga tanena kuti adaali ndi moto wosatha chifukwa cha

zinyalala zochuluka, anaperekedwa ngati chitsanzo cha “Hell” komwe munthu ankawonongedwako kwa muyaya – “*..kumene kuli moto wosazima, kumene nyongolotsi sizimafa* (sizimafa ngakhale kudaali moto!” [Marko 9:43,44 [onani kuti vesi 44 m’Baibulo la Chichewa mulibe!]). Liwu loti “Gehena” kwa anthu a chi Yuda, linali chikumbutso chachikulu chowonetsa kukanidwa ndi kutayidwa pamaso pa a Yuda anzawo komanso pamaso pa Mulungu wao. Munthu akaponyedwa m’dzenje la Gehena, kwa a Yuda aja, chidaali chizindikiro cha chionongeko cha moyo wake mpaka muyaya; Kudaali chizindikiro chosoweka kwa chipulumutso pamaso pa Yehova ndi Khristu Yesu. Taona kale kuti m’Gehena, munkakhala moto wosazimika chifukwa chakuti munkaponyedwa zinyalala ndi anthu akufa mopitirizika, ndipo izi, tawonanso kuti motowo ukuphiphiritisa mkwiyo wa Mulungu chifukwa cha tchimo, komanso pali chiphiphiritso cha chionongeko cha anthu ochimwa kudzera kuimfa, popeza monga tidziwa, “mphotho ya tchimo ndi imfa”.

Tikawerenga kuti “kumene nyongolotsi sizimafa”, tidziwanso kuti mau’wa akuyimira chiwonongeko chosatha. Tiona kuti nyongolotsi sizingatheke kukhala osafa m’chimoto choopsya ngati chimenechi. Choncho, mau amenewanso ndi chiphiphiritso cha chionongeko chachikulu chomwe chidzachitike ku matupi a anthu ochimwa chifukwa adzadyedwa ndi nyongolotsi kachiwiri akadzawukitsidwanso. Kotero, izi zinawonetsedwa momveka bwino popereka chitsanzo cha malo otchedwa “Gehena” omwe adaali kumbali kwa mzinda wa Yerusalemu.

MPATUKO 11: PURIGATORIYA

A tcharitchi cha chi Katolika amaphunzitsa otsatira awo ndi anthu ena kuti mizimu ya anthu a Mulungu ndi ena onse akafa amapita kumalo a chiyembekezo otchedwa “Purigatoriya” amene kwa iwo amati ndi nyumba yomwe inamangidwa pakati kati pa kumwamba ndi “Hade” (Hell). Iwo amapitiriza chiphunzitso chawo pomanena kuti malo amenewa ndiwo amene munthuyo amalangikako pang’ono, kenaka amakapatsidwanso mwayi wina kuti alape machimo ake ndipo kutinso akalapa, amatha kuloledwa kupita Kumwamba

(Heaven). A Chikatorika amanenanso kuti mapemphero, kuyatsa muuni (kandulo) ndi mphatso zimene anthu ena amapereka wakufayo atafa kale, zimathandiza munthu uja kuti akhale nthawi yochepa m'chilango chimene amapatsidwa ku Purigatoriya kuja. Tinene mosataya nthawi yaikulu pano kuti iri ndi bodza lokanika lomwe nkhani yake siyingapezeke pena paliponse m'Baibulo. Tiyenera kukumbukira nthawi zonse kuti ngati cholinga chathu nkuchita chifuniro cha Mulungu, tiyeni titsate zomwe Baibulo limanena ndipo Mulungu adzatiphunzitsa njira yeni yeni yolongosoka. Tiyeni choncho, tionere limodzi mfundo zotsatirazi:-

- Baibulo silikambapo kanthu kena kalikonse kokhudza malo ngati amenewa.
- Tawerenga ndipo tsopano tazindikira kuti “mzimu” (soul) ukutanthawuza “uthunthu” wonse wa munthu (kapenanso chinthu cha moyo) omwe ndi osiyana kwambiri ndi maganizo oti ndiko kanthu kena mkati kati mwa munthu kapena mwathupi lathu; Ndipo kuti “Hade” kapena “Hell” ndi “Manda” osati malo a chilango Kumwamba ayi.
- Olungama samalonjezedwa chipulumutso chawo kuti adzachepeza Kumwamba ayi. Ife tikamawerenga Baibulo, timamva kuti chipulumutso chidzaperekedwa pamene Khristu adzabwerenso panso pano kudzaweruza anthu ochimwa ndi okhulupirika ali pa Chimpando Chake Cha Ufumu. Apa zikuonekeratu kuti nkoyenera kuti Khristu adzabwerenso kotero, adzapulumutsedi anthu ake osati kuti ife tizipita kumwamba kukalandira chipulumutso chimenechi ayi, kutero ndiko kutsutsana ndi Malembo Oyera. Mwaichi, munthu samalandira chipulumutso pamene munthuyo wangofa nkukalowa “m'Purigatoriya” monga a Katorika amanenera ayi (Mateyu 25:31-34; Chibvumbulutso 22:12).
- Onse olungama adzalandira mphatso zawo nthawi imodzi, osati munthu aliyense kukalandira mphatso ya chipulumutso payekha

akangofa monga anzathu ena amanenera ayi (A Hebri 11:39,40; 2 Timoteo 4:8).

- Imfa inadza kwa munthu ndipo kuti munthuyo akafa, saadziwa chirichonse chochitika pakati pa iye ndi dziko lonse. Izi ndi zosiyana kwambiri ndi zimene chiphunzitso cha a Katorika pa za “Purigatoriya” chimanenera.
- Ife timayeretsedwa komanso kutsukidwa ku machimo athu kudzera mu ubatizo mwa Khristu Yesu ndiponso pokula ndi kuzama m’chikhulupiriro chathu pogwira ntchito yake ya Khristuyo m’moyo uno. Sizingatheke kotero, kuti tidzayeretsedwa titalangidwa kale pamene tidzafe ayi. Choncho, timalangizidwa kuti “*..Tsukani chotupitsa chakale*” cha uchimo m’miyoyo yathu (1 Akorinto 5:7); kuti tikayeretsedwe m’ntchito zathu ndi khalidwe la uchimo (2 Timoteo 2:21; A Hebri 9:14). Nthawi yoyeretsedwa yoyenera kotero, ndi ino, mu umoyo uno osati ku “Puligatoriya” kumene amati tidzapite tikadzafa ayi. “*...Taonani, tsopano ndiyo nyengo ya chipulumutso*” (2 Akorinto 6:2). Kumvera Mulungu Yehova, kwaife kudzera mu ubatizo komanso kukula ndi kukhwima mu uzimu m’moyo uno, ndiko kumene kudzatitengere ife ku mwayi wa chipulumutso chirinkudzacho m’nthawiyo (Agalatiya 6:8) osati kudikira kwa kanthawi kochepea “m’Purigatoriya” n’cholinga chakuti ena azitipempherera kuti kenaka tipulumutsidwe ayi.
- Ngakhale anthu ena ayatse miuni (makandulo), ena apereke zopereka zawo ku tcharitchi ya Chikatorika pofuna kupulumutsa miyoyo ya abale awo amene anafa kale, chodziwika ndi chakuti chipulumutso chidzatifika ife mogwirizana ndi ntchito zimene ifeyo payekha payekha tinachita. Ntchito zonsezi sizingasinthe china chirichonse pa chipulumutso chathu pamaso pa Yesu Khristu. “*...iwo akutama kulemera kwao; kuombola m’bale wao sangadzamuombole..., kapena kumpereka* (kuti akhale ngati) *dipo kwa Mulungu Yehova: ...Kuti akhale ndi moyo wosafa, Osaona chibvundi..*” (Masalmo 49:6-9).

MPATUKO 12: AZIMU NDI MIUKA

Chikhulupiriro chonena kuti munthu akafa, amakhalabe ndi moyo mu uthunthu wa nyama zina; Komanso kuti amakhala ndi mzimu umene amabadwa nawo, ndi chimodzi mwa zikhulupiriro zakale, chimene munthu ankakhutira nacho pofuna kukwaniritsa zolinga ndi zilako lako zake kuti anthu ena akhulupirirensa kuti munthu akafa amakhalabe ndi moyo mu uzimu naapita kumwamba.

Sitifuna kutaya nthawi kunena zambiri pa nkhanayi chifukwa takamba kale kuti, mzimu wa munthu ndiwo mpweya kapena tinene kuti umoyo wake mwaife anthu, umene umabwereranso kwa Mwini Mulungu Yehova ngati ife tafa (Mlaliki 12:7). Izi kotero, zikutanthawuza kuti mzimu wake wa munthu sumangoyenda yenda ngati “mzukwa”, komanso kuti sumalowa mwa nyama ina ya kutchire kapenanso mwa munthu wina monga ena amanenera, nkukhala ndi moyo kuti upitirizike umoyo wake padziko lino ayi. Aliyense waife payekha payekha, tidzaweruzidwa mogwirizana ndi ntchito zathu monga timawerenga m’Baibulo (2 Akorinto 5:10). Ngati mzimu wathu ndi mzimu wa munthu amene adaalipo kale masiku akalewo, ndiye kuti chiweruzo cha Mulungu ndi mphatso za Chiuta sizidzaperekedwa kwaife monga mwa ntchito zathu (Chibvumbulutso 22:12), komanso, sizingatheke kuti Baibulo limene ndilo Mau a Mulungu kunena zabodza ayi, ndipo ife tonse tikudziwa kuti Baibulo ndilodi Mau eni eni a Mulungu Yehova. Ife tikudziwa kuti zimene akuphunzitsa anthu ena monganso a Chikatorika aja sizoonza ayi chifukwa zikusiyana ndi zimene timawerenga m’Baibulo. Timakhulupirira kuti Baibulo ndilo Mau a Mulungu eni eni ndipo kuti zonse zimene zimasiyana ndi Mau amenewa, sizingakhale zoonza kwaife. Tiyenera tichenjere ndi anthu amene amakhala ndi luso lofuna kusokoneza Mau a Mulungu pomasulira Mau’wo molakwika dala n’cholinga chakuti anthu ambiri azisokera namawatsata iwo kuchiongeko.

Mzimu wa munthu umabwerera kwa Mulungu pamene munthuyo wafa ndipo kuti chikumbumtima chake chonse chimathera pomwepo. Choncho, ngati ife timafuna funa kulankhula ndi anthu akufa, ndiye kuti tikuwonetsa kusazindikira

kwathu konse pa chikonzero cha Mau a Mulungu wamoyo chomwe tingachipeze powerenga m’Baibulo lokha (Yesaya 8:19,20). Baibulo limalongosola bwino kuti munthu akafa, sangathenso kubwerera kunyumba yake, kapena ku mzinda wake wakwao ayi; Palibe kuti mzimu wake kapena muuko (mzukwa) wake ungate kumayenda yenda nkukazunza anthu achibale amene ali ndi moyo ayi. Kumangokhala kuwopsyezana chabe ndi zikhulupiro zotsutsana ngati zimenezi. Yobu 20:7-9 sakubisa chikhulupiro chimene iye payekha adaali nacho pa Malembo Oyera maka maka pokhudza mutu umenewu: “...(munthu) *adzatayika kosatha ngati zonyasa zake; Iwo amene adamuona adzati Ali kuti iye? Adzauluka ngati loto, osapezekanso; Nadzaingidwa ngati masomphenya a usiku...Ndi malo ake sadzampenyanso*” Ndipo Yobu 7:9,10 akunenanso kuti; “*Mtambo wapita watha, Momwemo wakutsikira kumanda sadzakweranso. Sadzabweranso kunyumba yake, Osadziwanso malo ake*”. Tikalola modzipereka ndi mozindikira kuti mau awa ndiwo Mau a Mulungu, tidzakhutira ndipo tidzautaya ulaliki onse wa bodza umene udazika mizu yozama m’mitima mwathu pokhudza nkhani imeneyi ya mizimu kapena mauka a anthu akufa; amenenso amati amazunza nyumba za abale aiwo eni akafa. Chikhulupiro chotere, ndicho “bodza” lomwe lija la “njoka” kwa Adamu ndi Heva m’ munda wa Edeni uja.

MPATUKO 13: IFE TIMAUKITSIDWA MU UTHUNTHU WOTANI?

Tadziwa kuti moyo wosatha komanso kusinthika kwathu kuti tidzakhale m’maonekedwe ndi m’makhalidwe a Mulungu patsiku la chiweruzo, udzaperekedwa kwaife ngati tikhulupirira choonadi mpaka komalizira pamene Yesu adzabweranso panso pano. Khristu adzawaukitsa anthu okhawa amene adzakhala ndi udindo wa Mau a Mulungu pa chiweruzo chake, kenaka adzawaweruzwa atawasonkhanitsa onse pamodzi. Poona kuti mphotho ya moyo wosatha idzaperekedwa pa tsiku lomaliza limene ndilo la chiweruzo, ndi zodziwikiratu kuti anthu amene adzawukitsidwe, adzawukitsidwa asanapatsidwe moyo wosatha kotero, adzatha kufanso kachiwiri ngakhale kuti adzakhala asanalandirebe mphotho ya moyo wosatha. Tionanso kuti akanakhala kuti

anthuwo adzawukitsidwa ali nawo kale moyo wosathawo, ndiye kuti sikukanakhala kofunikira kuti chiweruzo cha tsiku lomalizali chidzachitike ndipo kuti Yesu adzabwerenso kudzapereka mphotho kwa iwo okhulupirikawo.

Tidzalowa mu Ufumu wa Mulungu nthawi yomwe chiweruzo chidzachitike ndipo chikadzangotha Khristu ali pa Chimpando Cha Ufumu wa chiweruzo wake, anthu olungamawo adzasangalala (Mateyu 25:34); Okhulupirira onse choncho, saali mu Ufumu wa Mulungu lero lino popeza chiweruzochi sichingachitike. **“..thupi ndi mwazi sizingathe kulowa mu Ufumu wa Mulungu; (koterokuti,) ...tonse tidzasandulizidwa mkamphindi, ,,Pakuti chobvunda ichi chiyenera kubvala chisabvundi, ndi chaimfa ichi kubvala chosafa”** (1 Akorinto 15:50,51,53). Ndipo mwaichi, kusinthika kumeneku kudzachitika komanso kudzaperekedwa kwa anthu okhawo okhulupirikadi, olungama ndi ochita bwino pamene tsiku lomalizali, la chiweruzoli lidzafika; Chifukwa iri ndilo tsiku lokhalo limene Ufumu wa Mulungu udzalowedwe kwa onse oyenera kuwulandira. Ngakhale ziri choncho, Paulo akukamba za **“...kuukitsidwa kwa akufa”** pamene ankalankhula za **“kuukanso kwa akufa”** kumene ndiko kuukitsidwa kwa anthu olungama amene adzalandire moyo wosatha patangotha chiweruzo cha olungama ndi oyipa. Iye koterokuti, anazindikiradi kuti **“kudzakhala kuuka kwa olungama ndi osalungama”** (Machitidwe 24:15). Paulo anadziwanso kuti onse amene ali ndi udindo pamaso pa Mulungu (onse amene anamva Mau ake); **“..adzamva mau ake, nadzatuluka** (kuchokera m’manda) **amene adachita zabwino, ku kuuka kwa moyo; koma amene adachita zoyipa ku kuuka kwa kuweruza”** (Yohane 5:29).

Paulo ankalankhula kawiri kawiri za **“..kuukanso ku moyo”** pamene anakamba za “kuukitsidwa”. Olungama adzatuluka kuchokera m’manda awo “kuuka ku moyo” – potuluka m’maenje a m’nthaka, ndipo adzaweruzidwa napatsidwa moyo wosatha. Chikonzero chonsechi, ndicho “kuukanso ku moyo”. Paulo akufotokozanso za momwe iye ankayesetsera kukhala umoyo wake wachiyero m’chikhristu chake molimbika; **“..ngati nkotheke ndikafikire ku kuuka kwa akufa”** (Afilipi 3:11). Chifukwa chakuti ali ndi udindo wa Mau a Mulungu kuti akadziyankhire milandu yake payekha: kuti iye ndithu adayesetsa **“ndikafike ku kuuka kwa akufa** (nkukhala ndi moyo)” ndipo izi zitanthauza “kuukanso kwa akufa”.

Zitsanzo zina zowonetsa “kuukanso” kuti kukutanthawuza “kuukanso ku moyo” ndi zimene tingazipeze m’ndime izi:- (Luka 14:14) kuphatikizaponso Luka 20:35; Yohane 11:24; 1 Akorinto 15:21,42; A Hebri 11:35; Chibvumbulutso 20:6. M’Masalmo 17:15, Davide akunena zakuti iye adzalandira mphotho pamene “adzawukitsidwe”. Iye anali ndi chizindikiro chimenechi chodzawukanso kwa akufa, ndipo adadziwa zonsezi za “kuukanso” pamwamba podziwanso za chiweruzo kotero, anazindikira kuti zimenezi ziyenera kuyendera limodzi. Kugwiritsa ntchito mau onena kuti “kuukanso” monga pa 1 Akorinto 15 kukuthandiza koposa kufotokozerana zomwe zinalembedwa pa 1 Akorinto 15:52, **“...akufa adzawukitsidwa m’chisabvundi”**. Ndizodziwikiratu kuti liwu loti “akufa” nthawi zina limakamba za “akufa m’chiyero” (anthu amene adafa m’chikhulupiriro maka maka 1 Akorinto 15) amene adzawukitsidwe kuti adzalandire moyo wosatha pa tsiku la chiweruzo: 1 Akorinto 15:13,21,35,43; 1 Atesalonika 4:16; Afilipi 3:11; Chibvumbulutso 14:13; 20:5,6. 1 Atesalonika 4:16,17 akunenapo zochitika zitatu zimene zikugwirizana ndi kubweranso kachiwiri kwa Yesu Khristu:-

- 1) Khristu pobwera adzawoneka
- 2) Akufa adzawukitsidwa
- 3) Onse amene ali ndi udindo pa Mau a Mulungu ndipo kuti adzakhalabe ali ndi moyo pamene Yesu Khristu adzabweranso, adzawukitsidwa kuti apite ku chiweruzo cha Khristuyo.

Mphatso ya moyo wosatha idzaperekedwa ukadzangotha msonkhano umenewu wa chiweruzo (Mateyu 25:31-34; 13:41-43); Choncho, moyo wosatha wa muyaya sudzapatsidwa pamene anthu azidzawukitsidwa kwa akufa ayi, chifukwa choyambirira kuchitika chidzakhala kuukitsidwa, kenaka chiweruzo ndipo komaliza, kuperekedwa kwa mphotho ya moyo wosatha ndi imfa ya muyaya. Taonetsa kale kuti olungama onse adzalandira mphotho zawo nthawi imodzi osati mosiyana ayi (Mateyu 25:34; A Hebri 11:39-40). Zonsezi sizikanatheka kukanakhala kuti mphatso ya moyo wosatha ikanadzaperekedwa pa nthawi ya kuukitsidwa kwa akufa. Chifukwa chake ndi chakuti owukitsidwawo, adzakhala okhawa amene ali ndi udindo pamaso pa Mulungu,

amene adzayenera kuyankha zoyipa ndi zabwino zimene iwo anadziwa pamanso pa Mulungu, omwe motero, ndi anthu ochimwa kapena olungama mogwirizana ndi zimene iwo anamva mokhudza Uthenga Wabwino.

Tidziwenseo kuti kuzindikira ichi mu umunthu wathu ndi chinthu chobvuta kwambiri ngati sititsogoza Mulungu pa maphunziro athu a Mau a Mulungu; Ndipo kuti Yehova Chiuta wathu sangachite monga munthu achita kapena kuganiza ayi koma monga Iye M'mphamvu Zake anakonzera pa chilengedwe, komanso monga mwandondomeko yake. Zikhoza kutheka kwaife kunena za ndondomeko ndi kachitidwe ka zinthu zina zokhudza tsiku lakubweranso kwa Khristu, koma tizindikire kuti Mwini zonse anakonza kale mwa ndondomeko yake yomwe nthawi zambiri tiyenera kuyiphunzira powerenga mozama m'Baibulo. Kuukitsidwa kwa anthu akufa, kukufotokozedwa ngati kuti kudzachitika *"..mkamphindi, mkutwanima kwa diso pa lipenga lotsiriza"* (1 Akorinto 15:51,52). Nkofunikira kudziwa kuti nthawi patsikulo idzakhala yosiyana kwambiri ndi imene tikuyidziwa lero linoyi, maka maka kwa iwo amene adzaweruzidwe. Nzodziwikiratu kuti onse amene ali ndi udindo pamanso pa Mulungu Yehova, podziwa chimene Mulungu afuna iwo achichite, adzayenera kupereka dongosolo la moyo wao pamene adaali pano padziko lapansi kwa Khristu amene adzakhale pa Chimpando Chake Cha Ufumu wa Chiweruzo; Ndipo kuti adzakambirana ndi Oweruzayo (Yesu [Mateyu 25:44 etc; Mlaliki 3:17; 12:14; Luka 12:2,3; 19:23; Ezekieli 18:21,22; 1 Timoteo 5:24,25; Aroma 14:11,12]). Tikangoganizira za anthu amene amadziwa za Mau a Mulungu, anthu omwe tsopano tingawatchule kuti ali ndi udindo, tipeza kuti alipo ambiri; Koteru, tiona kuti **"mkamphindi"** kamene kakambidwako ndicho chinsinsi ndi mphamvu ya Mulungu choncho, chiweruzo cha anthu onsewa chidzachitika "mkamphindi" mwamphamvu imeneyi ya Yehova monganso mwandondomeko ndi chikonzero chakecho!

Poona kuti nthawiyo idzachepetsedwa monga tamva; anthu ena amaganizabe kuti mphatso ya moyo wosatha idzaperekedwabe nthawi yomwe iwo azidzawukitsidwayo, izi sizingakhale choncho, chifukwa chikonzero cha Mulungu chiripo kale ndipo kuti ndi chikonzero cha ndondomeko osati cha chisokonezo ayi. Koteru, "mkamphindi" tawerengako, Yehova adzakwaniritsa kulongosola chikonzero chakecho kuti chiweruzo chakecho chidzachitike anthu

atawukitsidwa, nawonekera pa Chimpando Cha Ufumu Cha Yesu Khristu wa Chiweruzochi. Mwachisomo chake, kudzaperekedwanso mphotho monga mwachikonzero chake. Chifukwa chaichi, 1 Atesalonika 4:16,17 amakamba za olungama kuti adzayitanidwa ku chiweruzo ndi mfuu wa lipenga ndi mau a m'ngelo wamkulu, pamene 1 Akorinto 15:52 akunena za lipenga lomwelo ngati kuti lidzamvekanso pamene anthu olungamawo azidzapatsidwa moyo wosatha: Ichi ndi chifukwa chake Paulo adaganizanso mofanana ndi mfundo yomweyi kuti kuukanso kwa akufa ndi chiweruzo ziyenera kuyendera limodzi (Afilipi 1:23) ndipo ndi chinthu chimodzidi.

MPATUKO 14: KUKWATULIDWA

Pali mbiri yomwe inafilitsidwa maka maka m'matcharitchi a chi 'Evanjeriko' kuti oyera mtima "adzakwatulidwa" kupita kumwamba pamene Khristu adzabweranso. Chkhulupiriro chimenechi chimagwirizana ndi maganizo onena kuti dziko lapansi lidzaphwasulidwa. Taonetsa kale mu Mpatuko wa Chisanu ndi Chitatu, kuti izi sizoonanso ndipo kuti sizingatheke. Tadziwanso m'Phunziro 4.7 kuti malo operekerako m'phatso ya moyo wosatha adzakhala panso pano osati kumwamba monga ena amanenera ayi, apa tiona monga m'mene tadziwerengera tokha kuti izi sizoonanso. Maganizo olakwika otere amakhalapo chifukwa cha kumasulira kolakwika kwa Mau a Mulungu komwe kumachitika powerenga 1 Akorinto 4:1,17: ***"...Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba Mwini Yekha ndi mfuu..., ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mu mlenga lenga, ndipo potero, tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse."***

Tikaganiza za kuopsya kokangamira ulaliki wathu pa mau opezeka m'ndime imodzi yokha ya m'Baibulo, tionjezerenso kuti m'ndime imene yawerengedwayi palibe liwu lomwe likunenapo kuti olungama onse adzapita kumwamba, tiona tokha kuti pali bvuto lalikulu pakati pa akhristu. Chimene tatolapo pano n'chakuti Khristu ndiye amene adzatsike kuchokera kumwamba pamene adzakhale asanakumane ndi Oyera mtima mlenga lenga. Khristu adzalamulira

kosatha pa Chimpano cha mfumu Davide m'Yerusalemu, ndipo tonse tidzakhala naye pa dziko lapansi. Mwaichi, sizingatheke kuti tikakhale mlenga lenga ndi Khristu kwa muyaya. Mlenga lenga ndi ma kilomita ochepa kwambiri kuchokera pansu pano poyerekeza ndi Kumwamba kweni kweniko, kotero, mlenga lenga sindiye kofanana ndi Kumwamba komwe ndiko kumene Mulungu amakhala.

Mau a m'chi Greek amene amasuliridwa kuti “kukwatulidwa” akutanthawuza kuti “kutsompholedwa pamene wina asakuzindikira” ndipo komwe munthu wakwatulidwayo akupita sikunafotokozedwe kweni kweni. Timawerenga pa Levitiko 6:4 ndi Deuteronomo 28:31 m'Baibulo la chi Greek momwe “kukwatulidwa” kukufotokozeredwa ponena za kuberedwa kwa katundu. Kunalembedwanso pa Machitidwe 8:9 kuti:- *“..Mzimu wa Ambuye unakwatula Filipino; ndipo mdindo sanamuonanso, pakuti anapita njira yake wokondwera... Koma Filipino anapezedwa ku Azota..”* Kukwatulidwa uku, kukuonetsa momwe Filipino anathawitsidwira kapena tinene kuti anasowera mwa Mphamvu ya Mzimu Woyera kuchoka pamalo ena kukafika malo enanso. Pamene Khristu adzabweranso, a udindo podziwa Mau a Mulungu Woyera adzasonkhanitsidwa pamodzi kumalo a chiweruzo; sadzasiyidwa kuti akapite okha ku chiweruzoko ayi. Zikhoza kutheka kuti popita kumalo a chiweruzoko anthuwo adzayenda mlenga lenga kuti akafike kumaloko. Ichi ndi chikonzero cha Namalengayo chimene ife anthu sitingachidziwe ayi.

Yesu anati *“..Pamene mwana wa munthu adzawonekera, ...padzakhala anthu awiri m'munda, m'modzi adzatengedwa ndi winayo adzasiyidwa”* (Luka 17:30,36). Izi zikuperekanso chithunzi thunzi chokwatulidwa ndipo mosazindikirika ndi anthu ena omwe ali pamalopo, mwachitsanzo, kuchotsedwa mwachangu. Akuphonzira ake a Yesu Khristu anafunsa, *“Kuti Ambuye? Ndipo anati kwa iwo, ‘Pamene pali mtembo (thunthu la munthu) pomweponso miimba (chiomba nkhang) idzasonkhanitsidwa”* (Luka 17:37). Monga ziomba nkhang zimawuluka mlenga lenga mosakayikitsa, kenaka n'kutela pa nthaka pomwe thupi la nyama kapena munthu lagona likuyamba kuwola, ndi momwenso zidzakhaliye ndi anthu a udindo m'Mau a Mulungu, omwe adzitere pa bwalo la chiweruzo kukumana ndi Ambuye wao Yesu Khristu. Tiyenera kunena motsimikiza komanso motsindika kuti mpando wa Chiweruzo wa Khristu Yesu

udzakhalapo; ndipo onse a udindo amene ndi anthu omwe anamva Uthenga Wabwino, adzawonekera pamaso pa Yesuyo, olungama onse asalandire mphoto zawo. Pongowerenganso 1 Atesalonika 4:16,17 nkwapatali kuganiza kuti onse a udindowo adzakwatulidwa kupita mlenga lenga, naakhala ndi Khristu mlenga lengamo nthawi zosatha. Koma m'malo mwake kenaka tadziwanso kuti onse a udindowa, adzasonkhanitsidwa pamodzi naadzakhala pamalo a chiweruzo, mwina poyendetsedwa mlenga lenga kukafika kumaloko; kenaka nkulandirano mphatso yawo ya moyo wosatha imene iwo akhala akuyiyembekezera.

PHUNZIRO 4: MAFUNSO

1. Chimachitika ndi chiyani munthu akafa?
 - (a) Mzimu umapita Kumwamba (b) Timakhala osazindikira chirichonse chochitika
 - (b) Mzimu umasungidwa kwina kwake mpaka tsiku la chiweruzo
 - (c) Mizimu yochimwa imapita ku Hade koma yolungama imapita Kumwamba

2. Mzimu n'chiyani?
 - (a) Mbali imodzi ya mkati mwathu yomwe siyimafa
 - (b) Liwu lomwe limanthawuza kuti “thupi, umunthu, chinthu cha moyo”
 - (c) Chimodzimodzinso ngati muzukwa
 - (d) Kena kake kamene kamapita Kumwamba kapena ku Hade pamene munthu wafa

3. Mzimu wa munthu n'chiyani?

4. Mwachidule, fotokozani za uthunthu ndi maonekedwe a munthu.

5. Lembani kapena fotokozani zinthu ziwiri zomwe zimaonetsa kuti imfa imabwere-tsa kusazindikira kwa munthu.

6. Mudziwapo chiyani pa za Mpando wa Chiweruzo wa Yesu Khristu?

7. Kodi ndi ndani amene adzawukitsidwe kwa akufa komanso kudzaweruzidwa-pamene Khristu adzabwerenso?

8. “Hade” kapena “Hell” n'chiyani?

9. Gehena n'chiyani?

Mukayankha chonde tumizani mayankho anu ku imodzi mwa ma adiresi alembedwa komali kwa buku lino:

PHUNZIRO 5

UFUMU WA MULUNGU

5.1 KUFOTOKOZERA ZA UFUMU WA MULUNGU

Maphunziro tangomalizawa, taonetsa kuti ndi cholinga cha Mulungu kupereka mphoto ya moyo wosatha kwa anthu ake olungama pamene Khristu adzabweranso. Umoyo wosatha umenewu udzakhala panso pano mu Ufumu wake; M'malonjezani ake, Mulungu sadanenepo kuti anthu ake adzapita kumwamba. Taphunzira kuti “...*Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu*” (Mateyu 4:23) unalalikidwa kwa Abrahamu kudzera m'malonjezani ake a moyo wosatha padziko lapansi lino mu uthenga wabwino umene unakambidwa kwa Abrahamuyo (Agalatiya 3:8). “*Ufumu wa Mulungu*” choncho, ndiyo nthawi

yomwe malonjezano a Mulungu adzakwaniritsidwe Khristu akadzabweranso padziko lino lapansi. Tikudziwa kuti Mulungu ndi Mfumu ya Mafumu a chilengedwe chonse cha dziko lapansi kufikira panopa; Iye anapereka ufulu kwa munthu kuti alamule dziko lapansi monga mwakufuna ndi chikonzero chake. Mwaichi, dziko lino tiri ndi “Maufumu a wanthu” (Danieli 4:17).

Pakubweranso kwa Khristu, **“Ufumu wa dziko lapansi wayamba** (udzakhala) **kukhala wa Khristu ndi Ambuye Wathu; ndipo adzachita** (adzalamulira) **ufumu kufikira kunthawi za nthawi”** (Chibvumbulutso 11:15). Kotero, cholinga cha Mulungu ndi zofuna zake zonse zidzachitika mwa kufuna kwake. Mwaichi, Yesu alamula kuti tizipemphera: **“Ufumu wanu udze,** (kuti) **kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba** (m’mene kuliri lero) **chomwecho pansi pano”** (Mateyu 6:10). Chifukwa chaichi, **“Ufumu wa Mulungu”** ndi Mau omwe amathanso kutanthawuzidwa kuti **“Ufumu wa Kumwamba”** (Mateyu 13:11; Marko 4:11). Onetsaninso kuti m’Baibulo sitimawerengamo Mau akuti **“Ufumu wokakhala kumwamba”** ayi; uwu ndi Ufumu wa Kumwamba kapena kuti Ufumu wochokera kumwamba ndipo udzakhazikitsidwa padziko lapansi lino ndi Khristu akadzabweranso. Monga cholinga ndi zofuna za Mulungu zonse zimachitika, ndipo kuti angelo onse amamumvera Iye, Chiuta sangakangane ndi iwo amene analengedwanso ndi Yehovayo (Masalmo 103:19-21), moteronso, zidzakhala choncho, ndi anthu onse mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo pamene onse okhalamo adzakhale olungama okha okha, amenenso panthawiyo, adzakhale “ofanana ndi Angelo” (Luka 20:36).

Kulowa mu Ufumu wa Mulungu pamene Khristu adzabweranso kotero, ndiko kumaliza kwa ntchito yathu yolemetsa yolimbana ndi mazunzo komanso tchimo m’moyo uno (Mateyu 25:34; Machitidwe 14:22); Mwaichi, nkofunikira kumvetsa komanso kuzindikira pa zonse zimene zikhudzana ndi “Ufumu wa Mulungu”. Ulaliki wa Filipino ponena za Khristu, ukutsamira pa mfundo yonena kuti iye (Filipo), **“...‘ankalalikirira,’** (zinthu zogwira mtima zokhudza ulaliki weni weni) **Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Khristu”** (Machitidwe 8:5,12). Pafupi fupi ndime zonse zimene zikufotokozera ulaliki wa Paulo kumalo osiyana siyana, zikunena za “Ufumu wa Mulungu” kuti ndiye mutu wa ulaliki wake wa Pauloyo (Machitidwe 19:8; 28:23,31). Choncho, n’chinthu chofunikira kwambiri kumvetsetsa mozindikira bwino za ulaliki wa

Ufumu wa Mulungu, poona kuti ndipamene pagonanso Uthenga Wabwino. *“Pakuti tiyenera ngakhale m’mazunzo kulowa mu Ufumu wa Mulungu”* (Machitidwe 4:17-22). Ngakhale tipeze mabvuto otani, anthu a Mulungu tiyenera kupirira mpaka pamene tidzayenezedwa kulandira mphoto yathu yapamwamba ndi chisangalalo.

Nebukadinezara mfumu ya Babulo, anafuna kudziwa za tsogolo la dziko lapansi (Danieli 2). Ndipo iye anaonetsedwa masomphenya a fano lopangidwa ndi zitsulo zosiyana siyana. Danieli anamasulira mutu wa fanizo la mfumu lija lomwe lidaali lopangidwa ndi golide kuti linkayimira kapena tinene kuti kutanthauzira mfumu Nebukadinezarayo (Danieli 2:38). Ndipo kuti ufumu wake ukadzatha, kudzabwera maufumu ena kumalo ozungulira Israeli, kumenenso iye ankalamulira, ndipo kwina konse kudzakhhalanso maufumu ena a mphamvu ndi ofooka monga Danieli akunena, *“...Ndi zala za mapazi, mwina zitsulo ndi mwina dongo, momwemo ufumuwo, mwina olimba mwina wogamphuka”* (Danieli 2:42). Izi zinali zodabwitsa kwa mfumu Nebukadinezara chifukwa iye sanayembekezere kuti ufumu wake ungadzathe.

Tikaona lero lino padziko lapansi, ulamuliro m’mayiko mwathu uli osiyana siyana, wina wamphamvu komanso wina ofowoka. Danieli kenaka, anamasulira za kamwala kakang’ono kamene kanaoneka, kakuomba mapazi a chifanizo chija, chimene chidaali chiyimire, kamwalako kadaphwasuliratu chifanizo chija. Chotsatira chake kamwalako kanayamba kukula kukhala chiphiri chachikulu chimene chidadzadza dziko lonse lapansi (Danieli 2:34,35). Pano tsopano mpamene tingazindikire kamwala kaja kuti kakuyimira Yesu Khristu (Mateyu 21:42; Machitidwe 4:11; Aefeso 2:20; 1 Petro 2:4-8). “Phiri” lomwe Yesu adzalipange apa ataphwasula maufumu onse a pa dziko lapansi lino likuyimira “Ufumu Wosatha komanso Wamphamvu wa Mulungu”, umene udzakhazikitsidwe pamene Khristuyo adzabwerenso. Uneneri umenewu paokha, ukutitsimikizira kuti ndithu, Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa padziko lapansi lino osati kumwamba monga ena amanenera ayi.

Kuti Ufumu wa Mulungu umenewu udzakhazikitsidwa ndithu pomwe Yesu Khristu adzabwerenso padziko lapansi lino, ndi mutu wina wapadera umene wafotokozedwa kale m’ malo ena a buku lomwe lino. Paulo akunenanso za Yesu

Khristu Oweruza anthu a moyo ndi akufa “...patsiku lakuonekera *Iye mu Ufumu Wake*” (2 Timoteo 4:1-5). Mika 4:1 akubvomerezanso mfundo yomweyi ya Danieli kuti Ufumu wa Mulungu udzakhala ngati chiphiri chachikulu “*Koma kudzachitika masiku otsiriza, kuti phiri la nyumba ya Yehova lidzakhazikika pamwamba pa mapiri; niidzakuzika pamwamba pa zitunda;*” kenaka chimene chikutsatira m’ndime imeneyi ndicho kufotokozerana momwe Ufumu Umenewu udzakhaliye padziko lapansi lino (Mika 4:1-4). Mulungu adzapereka kwa Yesu Khristu, Chimpando cha Davide pamene adaali pa ufumu mu Mzinda wa Yerusalemu: “*Iye adzakhala Wamkulukulu: ndipo Mulungu adzampatsa Iye mpando wachimfumu wa Davide atate wake. ...ndipo adzalamulira kunthawi zonse; ndipo Ufumu wake sudzatha*” (Luka 1:32,33). Apa Yesu Khristu ayenera kudzayambira nthawi iyi kulamulira pa Chimpando Chaufumu wa Davide. Iyi kotero, ndi nthawi imene Ufumu Wakewo udzayambike. Ndipo tsiku limeneri ndi lomwe Khristu adzabweranso. “*Ufumu Wake sudzatha*” tiona kuti zikugwirizana ndi Danieli 2:44: “*Ndipo masiku a maufumu aja Mulungu wa Kumwamba adzayika ufumu woti sudzaonongeka ku nthawi zonse, ndi ulamuliro wake sudzasiyidwa mtundu wina wa anthu,*”. Chibvumbulutso 11:15 akukamba mofanananso pofotokozerana zimene zidzachitika panthawi yomwe Khristu adzabweranso kuti “*Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye Wathu, ndi wa Khristu, ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi*”. Apanso paonekeratu kuti Mulungu adakhazikitsa kale chikonzero cha m’mene zinthu zonse zidzayendere kutsogolo kwa nthawi ino; ndipo kuti nthawi zimene zonsezi zidzayambike ndi chitsimikizo chakufupikira kwakubweranso kwachiwiri kwa Yesu Khristu padziko lapansi lino.

5.2 UFUMU WA MULUNGU SUNAKHAZIKITSIDWE

Maganizo amene alipo m’matcharitchi ena a lero ndi onena kuti Ufumu wa Mulungu ulipo pakati pawo ndipo kuti akhristu a matcharitchi amenewa, ndi

amene akukhala mu Ufumuwo. Tikudziwadi kuti onse okhulupirira eni eni adzapatsidwa malo ngati mphotho yawo mu Ufumu wa Mulungu, ndipo kuti ichi ndicho chiyembekezo chathu cha mtsogolo kwa munthu aliyense amene akupembedza kudzera mwa Yesu Khristu woonayo. Tikudziwanso kuti izi zidzachitika pamene Khristuyo adzabwerenso kudzakhazikitsa Ufumu wa Mulunguwo.

Tikatenga zomwe taphunzira tsopano, taona kuti zoonadi, **“...thupi ndi mwazi sizingatheke kulowa mu Ufumu wa Mulungu”** (1 Akorinto 15:50). Ife ndife **“osauka adziko lapansi... (koma) olemera ndi chikhulupiriro ndinso olowa nyumba ya Ufumu umene adawulonjeza kwa iwo a kumkonda Iye”** (Yakobo 2:5), popeza ubatizo umatikonza ife kuti tikhale oyenera pamaso pake ndi oyenera kulandira nawo malonjezano a kwa Abrahamu; Malonjezano amene ali okhudza za Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo (Mateyu 4:23; Agalatiya 3:8, 27-29). Ndipo kotero, sichinthu chachilendo kumva za malonjezano olandira mpatso yokhala nawo mu Ufumu wa Mulungu pamene Khristu adzabwerenso. Chifukwa chake n’chakuti, iyi idzakhala nthawi yokhayo yomwe malonjezano a kwa Abrahamu adzakwaniritsidwe (Mateyu 25:34; 1 Akorinto 6:9, 10; 15:5; Agalatiya 5:21; Aefeso 5:5). Tikangowerenga m’Baibulo, timamveratu kuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa Yesu Khristu akadzabweranso ndipo kuti izi, zikuonetseratu kuti Ufumuwo sunakhazikitsidwebe popeza tonse tikudziwa kuti Khristuyo sanabwerenso padziko lapansi lino.

Yesu adapereka fanizo lake pofuna kukonza maganizo olakwika a anthu ena amene adaali ndi chithunzi thunzi choti Ufumu wa Mulungu uwoneka kwa iwo mwamsanga. Choncho, Iye ananena za **“..munthu wina wa mfuko lotchuka amene adapita kudziko lakutali, kuti akadzilandirire yekha Ufumu, kenaka n’kukabwererako.”** Panthawi imeneyi, anasiya akapolo ake nawapatsa maudindo osiyana siyana kuti ayang’anire chuma chake. **“Ndipo kunali pakubwera iye, atalandira Ufumuwo, anati ayitanidwe kwa iye akapolo aja”** kuti aweruzidwe monga iwo anachita m’maudindo awo amene anapatsidwa kwa iwo (Luka 19:11-27).

Zikuonekeratu kuti apa wamfuko lotchuka uja akuyimira Ambuye wathu Khristu, amene ***“anapita kudziko lakutali”*** Kumwamba kukalandira Ufumu Wake kwa Mulungu. Ndipo kuti adzabweranso mu ulemerero wake pamene adzaweruze dziko lapansi. Mwaichi, tiona kuti palibe amene adalandira kale Ufumu wa Mulungu mpaka Yesu Khristu adzabwerenso padziko lapansi.

Manunsu otsatirawa akutitsimikiziranso za mfundo yomweyi momveka bwino:-

- ***“Ufumu wanga siuli wa dziko lino lapansi..,(siuli wa nthawi ino)”*** Yesu pano akunenetsa momveka bwino (Yohane 18:36). Komabe, onaninsu kuti ngakhale nthawi imeneyi, Yesu adaanenabe kuti ***“Munena kuti ndine Mfumu, Ndinabadwira ichi Ine,”*** (Yohane 18:37), chomwe chikuonetseratu kuti Ufumu Wake Khristu, sanayambe kulamulira pa nthawiyo, kapenanso panopa ayi, koma kuti adzalamulira nthawi yake ikadzakwana. N’chifukwa chake, ngakhale okhulupirira oyambirira m’chirumika choyamba akukambidwa ***kuti “..anali kuyembekezera Ufumu wa Mulungu”*** (Marko 15:43).
- Khristu anawawuza akuphunzira ake kuti sadzamwanso chikho cha vinyo ***“..Ndipo ndinena kwa inu, sindidzamwanso chipatso ichi cha mphesa kufikira tsiku limene ndidzamwa chatsopano, pamodzi ndi inu mu Ufumu wa Atate Wanga.”*** (Mateyu 26:29). Izi zikuonetseratu kuti Ufumuwo udzakhalapo mtsogolomo osati panopa ayi. Umu ndi m’mene anthu ankamvera za Uthenga Wabwino wa Khristu kalelo, Uthenga wosangalatsa wa Ufumu wa Mulungu (Luka 8:1). ***“Wodala iye, amene adzadya mkate mu Ufumu wa Mulungu”*** ndi ndemanga imene akhristu oyambirirawo ananena pa mfundo imeneyi ya Ufumu wa Mulungu (Luka 14:15).
- Luka 22:29,30 akutsimikiziranso mfundo yomweyi ponena ***kuti “..Ndipo Ine ndikuikirani Ufumu monga Atate anga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu Wanga”***.
- Yesu anakambanso za zizindikiro zimene zidzawoneka pa dziko lapansi pakadzangokhala kanthawi pang’ono kuti Iye abwerenso ndipo anapheranso ndemanga iyi ***“..Inde chotero inunso, pakuona zinthu izi zirinkuchitika, zindikirani kuti Ufumu wa Mulungu uli pafupi”*** (Luka 21:31). Ndime imeneyi ingakhale yopanda

tanthawuzo lero ngati Ufumu wa Mulungu udakhazikitsidwa kale pakati pathu pano pamene Yesu Khristuyo asanabwere.

- **“...tiyenera kulowa mu Ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri”** (Machitidwe 14:22). Kotero, sichachilendo kuona kuti okhulupirira owona eni eni a Mulungu, amayesetsa kupemphera m’chilungamo kuti **“Ufumu wa Mulungu”** udze msanga (Mateyu 6:10).
- Mulungu **“ayitana inu mulowe Ufumu wake wa Iye yekha”** (1 Atesalonika 2:12); ndipo pofuna kuonetsa kumvera kwathu, tiyeni tisake sake khomo la Ufumulo m’chipembedzo choyenera chauzimu wa chi Mulungu pakati pathu tsopano lino (Mateyu 6:33).

UFUMU WA MULUNGU ULI MKATI MWA INU?

Ngakhale pali chitsimikizo chokwanira m’ndime ziri pamwambazi pa nkhani ya Ufumu wa Mulungu, matcharitchi ambiri amakakamirabe pa chiphunzitso chonena kuti “Ufumu wa Mulungu uli mkati mwanu” mwina chifukwa chosamvetsa bwino pamene amawerenga (Luka 17:21). Mau’wa anamasuliridwa mokhozeka m’ma Baibulo ena motere:- **“Ufumu wa Mulungu uli pakati pa inu”** (Onani Baibulo la ‘Authorised Version’ mg.). Apa zikuonetsa kuti Yesu ankalankhula kwa Afalisi amene panthawiyo adaali pamalopo (ndime 20); **“inu”** kotero, akukamba za anthu amene adaalipo pamalopo nthawi imene Yesu Khristu ankalankhula Mau’wa osati kwa ife anthu a lero lino ayi. Sizinkatanthawuza akhristu okhulupirira amene alipo lero ayi koma iwo amene ankamva Yesu akulankhula za nkhanayi panthawiyo chifukwa chakuti Yesu adalidi ndi iwo pomwepo. Izi sizinatanthauze kuti Ufumu wa Mulungu unakhazikitsidwa m’mitima mwa anthu omwe ankamverawo ayi, koma kuti Yesu ndi amene mtsogolomo, adzathe kubweretsa Ufumuwo, choncho, popeza Yesuyo adaali pomwepo, iwo adaayenera kumvetsa ndi kukhulupirira zimene Yesuyo ankawauza. Onani kuti Yesu sanalamulirepo mu Ufumu wa Mulungu ngakhale dziko lapanasi; koma Baibulo limanena kuti Iye adzalamulira. Kotero, ngati apa nthawi inali isanakwane kuti Yesu alamulire, ndiye kuti sizingatheke kuti Ufumu wa Mulungu ukhazikitsidwe chifukwa zikanatero, ukanakhala ufumu wopanda Yesu Khristu!

A Yuda aja tidziwe kuti ankadzionetsera kwa anthu kuti iwo ndi amene amachita chilungamo pamaso pa Mulungu pofuna funa Mesiya (Mpulumutsi). Mu

Uthenga umenewu wa padera, zikuonetsa kuti “Ufumu wa Mulungu” unkatanthawuzidwa kuti ndilo dzina la Mesiya poona kuti Iye ndi amene adzakhale Mfumu ya mafumu, mu Ufumu wa Mulunguwo. Nchifukwa chake tikawerenga pa Marko 11:9, 10; pamene Yesu ankalowa mu Yerusalemu, timamva kuti anthuwo ankayimba mopfuula naati “*..Hosana, Hosana, wolemekezeka Iye (Mesiya) wakudza mdzina la Ambuye: Wolemekezeka Ufumu ulinkudza, wa Atate Wathu Davide; Hosana, Hosana, m’Kumwamba mwamba*”. Izi tiona kuti liwu loti “Mesiya” ndi loti “Ufumu” onse akuyendera limodzi m’nyimbo imeneyi. Koteronso, Yohane Mbatizi, analalikira kuti “*Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Pakuti uyu ndiye (Mesiya) ananenayo Yesaya Mneneri...*” (Mateyu 3:2,3). Pa Luka 17:20-24 tamvanso kuti Yesu anawayankha a Falisi ndi ena onse ponena za nthawi yobwera Ufumuwo kuti “*..Ufumu wa Mulungu*” uyenera kubwera pamene tikambanso za “*Kubweranso kwa Mwana wa munthu*” kutanthauza kuti pamene tikunena za kubwera kwa Ufumu wa Mulungu, tikukambanso za kubweranso padziko lapansi lino kwa Mwana wa Mulungu.

Mfundo ya Khristu apa inali yonena kuti a Yuda ankatanganidwa kwambiri ndi kudzionetsera pamaso pa anthu kuti iwo ndiwo amene adzamuone Mesiya koyamba ena onse asanamuone komanso asanazindikire kuti Mesiya’yo wafika; Koma sanathe kudziwa kuti Mesiya amene akumufuna funayo ndi Yesu amenenso adaali naye kale pakati pawo. Sanathe kudziwadi kuti “Ufumu wa Mulungu” udaali pakati pawo pomwepo popeza “Ufumuwo” ndiye “Yesu Khristu” yemwe adaali pakati pawopo mwa Khristu’yo ngakhale kuti pamaso pawopo ankaoneka monyozeka. Chifukwa chaichi, Yesu anawadzudzula kuti “*..Ufumu wa Mulungu (Mesiya) sukudza ndi maonekedwe akunja...ndipo sadzanena, Taonani uwu, kapena uwo! Pakuti tawonani, (Yesu Khristu) Ufumu wa Mulungu (Ambuye Yesu) uli mkati mwa inu*” (Luka 17:20,21). Mwachitsanzo, adayenera kukhulupirira kuti amene adzabweretse Ufumu wa Mulungu ali pakati pawo. Yesu ndiamene adaali chiphiphiritso cha Ufumu wa Mulungu pakati pawo pa nthawi imeneyi.

5.3 UFUMU WA MULUNGU KALELO

Ufumu wa Mulungu ndiyo mphatso yomwe idzalandiridwe ndi anthu okhulupirira onse. Mwaichi, ndi zonyaditsa komanso zolimbikitsa kwa anthu onse okhulupirirawo kuti atengerepo chitsanzo cha Khristu chimene chiri chinthu chaching'ono koposa kwa iwo kuti azunzike ndi kubvutika kwa nthawi yochepa monga Khristu'yo adachita. Nzodziwikiratu kuti anthu okhulupirira onse lerolino akuyembekezera nthawiyo ndi chilakolako chachikulu koteru, tsiku ndi tsiku, anthuwa amanthunthumira kuyesa yesa kuti azindikire kwathunthu Mau a Mulungu. Iwo amayesetsa kukhala tcheru poyang'anitsitsa maso awo patsogolo osabwerera m'mbuyo pa ntchito yawo yopembedza Mulungu wao mwa Khristu Yesu. Tsiku limeneri ndi tsiku lomwe iwo adzakumbutsidwe za ntchito yawo yolemetsa komanso za chipiriro chawo cholimba pamene anaonetsa chikondi chawo ndi chikhulupiriro chawo kwa Mulungu wawoyo amenenso akhala akumukonda ngati Tate wao weni weni.

Mau Opatulika amatipatsa ndondomeko yonse yokhudza Ufumu wa Mulungu ndipo zikhoza kutitengera ife moyo wathu onse kuti tizindikire chindunji chimenechi. Njira imodzi imene tingadziwire zinthu zina m'ndondomeko imeneyi ndiyo kuzindikira kuti Ufumu wa Mulungu udaalipo kale mdzina la Mfuko la ana a Israeli. Ufumu umenewu, timawerenga kuti udzakhazikitsidwanso pamene Khristu adzabweranso padziko lapansi. Baibulo likutiwunikira za Ufumu wa Mulungu umenewu kudzera m'ndondomeko ndi chikhalidwe cha mfuko la ana a Israeli amene akuphiphiritisa Ufumu weni weni wa Chiuta Mulungu Wathu. Ufumu wa ana a mfuko la Israeli masiku amenewo, ndicho chitsanzo chathu lerolino cha Ufumu wa Mulungu mtsogolomo pamene Khristu adzabweranso padziko lapansi.

Mulungu kawiri kawiri amatchulidwa mowirikiza pafupi pafupi pamene “Ufumu wa ana a Israeli” utchulidwanso m’Baibulo (Yesaya 44:6; cp.41:27; 43:15; Masalmo 48:2; 89:18; 149:2); Koteru, anthu a mfuko la Israeli ndiwo adaali **“Ufumu wa Mulungu”**. N’chifukwa chake, pamene anthu a ku Israeli adafuna kuti akhale ndi mfumu yawo yawo monga mafuko ena adaaliri, Mulungu anayankha Samueli naanena *kuti* **“..popeza sindiwe anakukana, koma ndine**

anandikana, kuti ndisakhale Mfumu yawo,” (1 Samueli 8:7). Tione pano kuti anthu amenewa (ana a Israeli) anayamba kukhala mu **“Ufumu wa Mulungu”** pamene anapangana chipangano ndi Mulungu pa phiri la Sinai atangosiyana ndi a Aigupto m’Nyanja ya Mchere (Eksodo 19). Pobvomereza, kuonetsa chikondi chawo kwa Mulungu, a Israeli analonjeza **“...kudzayasedwa** (kwa Mulungu) **ufumu wa Yehova ndi mtundu wopatulika”** (Eksodo 19:5-6). Mwaichi, **“..M’mene Israeli anatuluka ku Aigupto Nyumba ya Yakobo kwa anthu a chinenedwe chachilendo; Yuda anakhala malo ake a oyera, Israeli Ufumu Wake”** (Masalmo 114:1,2). Utatha mgwirizano umenewu, Israeli anachoka ku Sinai kuja n’kukakhala ku Kanani. Monga Mulungu adaali Mfumu yawo, iwo ankayang’aniridwa ndi **“Oweruza”** (ngati Gideoni ndi Samsoni) – m’ malo mokhala ndi mafumu awo. Anthu amenewa ankakhala ngati a mkhala-pakati, pakati pa Mulungu ndi ana a Israeli ndipo kuti panthawi ina yomwe inkapatulidwa ndi Mulungu, Oweruza m’modzi amatha kuyang’anira mbali ina ya mfuko la Israeli osati dziko lonse ayi. Oweruza ankalamulanso motsogozedwa ndi Mphamvu ya Mulungu pofuna kuthandiza ana a Israeli kukwaniritsa zofuna za Mulungu wao ndinso kuti iwo abwerere ku machimo awo; Kutsogolera ana a Israeli kuti agonjetse adani, ndintchito zina zimene iwo ankatha kupatsidwa ndi Mulungu panthawi yopatulidwa ndi Yehova’yo. Pamene ana a Israeli adafunsa Oweruza Gideoni kuti akhale Mfumu yawo, iye anawayankha kuti **“..Sindizalamulira inu, ngakhale mwana wanga sadzalamulira inu; Yehova adzalamulira inu”** (Oweruza 8:23).

Oweruza omalizira adaali Samueli. M’nthawi imeneyi, ana a Israeli anafunitsitsa kukhala ndi Mfumu yawo mwaiwo okha iwo eni monga mapfuko ena adaaliri (1 Samueli 8:5,6). M’mbiri yawo yonse ya ana a Israeli mpaka lero, anthu a Mulungu’wa akhala akuyesedwa kuti azifanana m’maonekedwe, zochita zawo ndi chikhalidwe chawo ndi anthu ena omwe ali pafupi nawo amenenso salabadira kupembedza Mulungu m’choonadi. Mayesero amene’wa akukula koposa maka maka m’masiku athu ano pamene anthu akufuna funa kusintha pa kachitidwe ka zinthu zosiyana siyana kuphatikizapo ndale za mayiko. Mulungu anamvanso chisoni ndi nkhani zotere ndipo anadandaula kwa Samueli, **“..anandikana kuti ndisakhale Mfumu yawo”** (1 Samueli 8:7,8). Komabe Mulungu ndi wachikondi, ndipo chifukwa chachikondi chakecho, anawapatsa mafumu osiyana siyana motero, oyambirira adaali Mfumu Sauli. Atafa Mfumu

Sauli wochimwayo, kunabwera Davide olungama ndi ena ambiri. Mafumu olungama ankazindikirabe kuti mpfuko la Israeli linaalibe mu ulamuliro wa Ufumu wa Mulungu ngakhale kuti iwo adaakana Ufumu Wakewo. Kotero, iwo ankazindikirabe kuti ulamuliro wao udakhazikitsidwa kuti iwo ngati mafumu, atsogolere mwanzeru ana a Israeli m'malo mwa Yehova Mwini ndi Mlengi wao.

Tikamvetsa mpfundo imeneyi, tikhoza kuzindikira bwino za Ufumu wa Solomoni, mwana wa Davide amene adaali pa ulamuliro wa “...mpando wachifumu Wake (wa Mulungu) mukhale Yehova Mulungu wanu mfumu pa anthu ake” (2 Mbiri 9:8; 1 Mbiri 25:5; 29:23). Ulamuliro wa Solomoni unaali wa mtendere komanso wachitukuko chosaneneka ndipo ulamuliro umenewu, ukuloserera za m'mene Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo, udzakhalire. Ichi n'chifukwa chake Yesu Khristu, ananena kuti Iye ndi Mfumu yomwe ikuyimira Ufumu wa Mulungu pa Chimpando Cha Ufumu Wake ngati ufumu wa Israeli wa chipembedzo choyera ndi choonadi (Mateyu 27:37, 42; Yohane 1:49; 12:13). Mafumu ambiri olungama amene adalembedwa m'Chipangano Chakale akuonetsa kuti ankasangalala kwambiri ndiponso kuti ankalandira m'dalitso waukulu akamalamulira ana a Mulungu m'chiyero. Izi zinkaloserera momwe zinthu zidzakhalire mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo. Choncho, zambarizi zikuloseradi m'mene Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo udzakhalire. N'chifukwa chake, monga Solomoni anamanga nyumba yopemphereramo mkati kati mwa Mzinda Wa Yerusalemu, Khristu adzamanganso kachisi wa chipembedzo (Ezekieli 40-48). Hezekiah ndi Solomoni monga adalandira m'phatso zosiyana siyana kuphatikizapo ulemu waukulu kuchokera m'mayiko onse oyandikana pa dziko lino lapansi (1 Mafumu 10:1-4; 2 Mafumu 20:12), ndipo iwo anaona ndi maso awo dziko la Israeli likudalitsika ndi chonde komanso kubala chitukuko chachikulu (1 Mafumu 10:5-15; Yesaya 37:30), iwo anazindikiranso kuti Ufumu wa Khristu wa dziko lonse lapansi udzadalitsika niudzabala zipatso zokoma zonsezi zimene zidaoneka kalezo panthawi yomwe iwo ankalamulirayo.

UKWATI

Ngakhale kuti Solomoni adayamba bwino ulamuliro wake kuchokera pa ubwana wakewo, iye anadzakwatira akazi osiyana siyana mosatsata chikonzero cha Mulungu, anakwatira mwachikunja ndipo izi ndi zimene zidamukokera ku machimo pamene anakakula. “*Ndipo mfumu solomoni anakonda akazi ambiri a*

chilendo,... akazi aku Moabu, ndi ku Amoni, ndi a ku Zidoni,... a mitundu ija Yehova adanena ndi ana a Israeli za iwo, kuti 'inu musakalowa kwa iwo, ndipo iwo asadzalowe kwa inu; zedi adzatembenuza mitima yanu kutsata milungu yawo; amenewo Solomoni anawaumirira kuwakonda. ...ndipo akazi ake anapambutsa mtima wake atsate milungu ina; ndipo Solomoni anachita choyipa pamaso pa Mulungu. ...Ndipo Yehova anakwiya ndi Solomoni popeza mtima wake unapambuka kwa Yehova Mulungu wa ana a Israeli ...koma iye sanasunga chimene Yehova anachilamula. Chifukwa chake, Yehova ananena ndi Solomoni, popeza chinthu ichi chachitika ndi iwe, ndipo sunasunga chipangano changa ndi malemba anga amene ndinakulamulira, zedi, ndidzakung'ambira ufumu ndi kuupatsa m'nyamata wako.” (1 Mafumu 11:1-11).

Kugwa kwa Solomoni chifukwa cha machimo amenewa kunawoneka m'khalidwe lake pafupi fupi m'moyo wake onse. Kudziwana kwake ndi akazi amene anali asanaonepo kufunikira kwake kwa chipembedzo chake chomwe ndi chipembedzo changwiro cha Mulungu wooka wa Israeli, ndiko kunapangitsa kuti Solomoni achitire chisoni zipembedzo zinazo zimene zinali zachikunja. Chikondi chake kwa akazi amenewa chinkatanthawuza kuti iye adaayenera kukondanso zipembedzo zawozo. Chikondi chake kwa azimayiwo chinamutseka m'maso kotero, sanathenso kuona kuti milungu inayo inali yotsutsana ndi chipembedzo cheni cheni choonadi cha Yehova wa ana a Israeli. Patapita nthawi yaitali, mu mtima mwake sanathenso kuzindikira kufunika kwake kopembedza Mulungu m'modzi woonadi wa Israeli. **“Mtima wake unadetsedwa”**, mwachitsanzo, adalibe nthumazi yosiyantsa pakati pa tchimo ndi chilungamo, kapena kusiyantsa pakati pa Mulungu Woyera ndi mafano opangidwa ndi munthu. Iye sanathe tsopano kudzipereka kwa Yehova Mulungu wake yemwensho amaadana koposa ndi **“zonyansa pamaso pa Mlengi Mulungu Wamoyoyo”**, chomwe chinakwiyitsa Chiuta mpaka kumutaya Solomoni chifukwa cha tchimo lake. Kumbukirani nthawi zonse kuti, ana a Israeli nthawi ndi nthawi, ankawakumbutsa Mulungu kuti iwo sayenera kukwatirana ndi akazi a mitundu yozungulira dziko lawo popeza anali achikunja (Eksodo 34:12-16; Yoswa 23:12,13; Deuteronomo 7:3).

Ife tikabatizidwa mwa Khristu, timasandulika kukhala amodzi mwa ana a Israeli. Ngati sitinakwatire kapena kukwatiwa pamene tinkabatizidwa, tiyenera tikwatire kapena tikwatiwe mwa ana a Israeli anzathu amene ndi Israeli wa chipembedzo choonadi cha Mulungu weni weni. Tikwatire ndi kukwatiwa mwa Ambuye (1 Akorinto 7:39) – mwachitsanzo, kwa obatizidwa anzathu mwa Khristu Yesu. Ngati tinakwatiwa kapena kukwatira kale tisanabatizidwe, tiyenera tisawaleke apabanja athu, banja lathu lidzayeretsedwa komanso lidzadalitsidwa ndi chikhulupiriro chathu mwa Khristu (1 Akorinto 7:12-14). Kukwatira dala munthu amene alibe chikhulupiriro choyenera, amenenso sanabatizidwe mwandondomeko yoyenera ya choonadi, nkuchimwa komanso kukwiyitsa Yehova Namalenga ndipo chotsatira chake ndi kukanidwa pamaso pa Mulungu. Solomononi anaonetseratu kuti sanamvera Yehova, iye anapereka chithunzi thunzi chonyozera malangizo ndi machenjezo a Mulungu pankhani ya akazi aja: “*..zedi adzatembenuza mitima yanu*” (1 Mafumu 11:2; Eksodo 34:16). Ndimitima yodziletsa yokha ndinso luntha lathu pa chipulumutso chimenechi imene ingatilekanitse ife ku chionongeko ndipo tidzapulumuka ku phompho loopsya’lo.

Taonetsa kale momwe akhristu ena samathera kuzindikira choonadi cheni cheni ndipo kotero, sangathenso kufananiza ndi kuona kugwirizana kwake pakati pa chikhulupiriro choonadi cha a Yuda ndi chikhristu. Samamudziwadi Mulungu wa Israeli wa moyoyo m’choonadi. Kukwatirana ndi anthu otere kumatibwezeretsadi m’mbuyo pachikhulupiriro ndi chipulumutso chathu. Chifukwa cha chimenechi, tiona kuti Isake ndi Yakobo adayenda ulendo wautali kupita kwao kumene anakapezako akazi oyera, oyesa yesa kuyenda m’chilungamo choonadi amene iwo akanawakwatira. Ndipo tionenso kuti Isake anadikira mpaka kufika zaka 40 zakubadwa ndi chifukwa chofunitsitsa kupeza mkazi wolongosoka (Genesis 24:3,4; 28:1). Timawerenganso kuti Ezra ndi Nehemiya anadandaula koposa atamva kuti panali a Yuda ena amene anakwatira akazi omwe sanali a Yuda, komanso anali osalongosoka. Izi zonse zikuonetsa kuti tchimo limeneri ndi loopsya pamaso pa Mulungu (Ezra 9:12; Nehemiya 10:29,30).

Mfundo imenemeyi tayikamba pano pofuna kuthandizana inu ndi ife kuti tonse tiziganizira pa zakufunikira kosunga chiyero pamaso pa Mulungu. Mutu wa “ukwati woyenera” wakambidwa kale mwa chindunji m’Phunziro 11.4.

CHIWERUZO CHA MULUNGU

Chifukwa chakuti Solomoni anachimwa, Ufumu wa ana a Israeli unagawidwa pakati: Mwana wa Solomoni, Rehabiamu, adalamulira mfuko la Yuda, Benjamini komanso theka la mfuko la Manase; Pamene Yeroboamu adalamulira mafuko khumi otsalawo. Ufumu wa mafuko khumi amenewa ndi amene ankatchedwa Israeli kapenanso kuti Efraimu, pamene Ufumu wa mafuko awiri ena aja ankadziwika ndi dzina loti 'Yuda'. Anthu onse m'mafuko amenewa anatsatira chitsanzo choyipa cha Mfumu Solomoni – iwo ankanena kuti amakhulupirira Mulungu wao m'choonadi pamene ankapembedza milungu ina yomwe mayiko ozungulira iwo ankayigwadira. Mulungu ankawadzudzula pafupi pafupi kudzera mwa aneneri, kuti asinthe makhalidwe awo oyipa, auchimo koma izi sizinatheke. Chifukwa chaichi, Iye anawalanga iwo powathamangitsa mu Ufumu wao wa Israeli, ndipo anatengedwa mu ukapolo nakakhala m'mayiko a adani awo kwa nthawi yaitali. A Assuri ndi a Babulo ndi amene anathira nkhondo yawo yodetsa mtima bii m'dziko la ana a Israeli chifukwa cha kusamvera kwao, ndipo ana a Israeli anagonjetsedwa natengedwa ngati akapolo: ***“Koma (Mulungu) munawalekerera zaka zambiri, ndi kuwachitira umboni ndi Mzimu wanu (Mau anu) mwa aneneri anu, koma sanamvera; chifukwa chake munawapereka m'dzanja la amitundu ya anthu a m'dziko (amitundu)”*** (Nehemiya 9:30).

Ufumu wa mafuko khumi aja a Israeli kunalidi mafumu oyipitsitsa. Yerobiamu, Ahabu, Yeohazi ndi ena otero, analembedwa m'buku la mafumu ngati anthu amene anatsogolera ana a Israeli kupembedza mafano koposa ena alionse. Mfumu yawo yomaliza idaali Hoseya ndipo idaali nthawi ya ulamuliro wake pamene mfuko la Israeli lidagonjetsedwa ndi a Assuri kotero, mafuko khumi a ana a Israeli anatengedwa ku ukapolo (2 Mafumu 17). Kuchokera pamene, sanathenso kubwerera kwaoko.

Mafuko awiri otsalawo, amene adaali mu ulamuliro wa ufumu wa Yuda, anaali ndimwayi wokhala ndi mafumu abwinopo monga Hezekiya ndi Yosiya, ngakhale kuti anthu awo ankachitabe choyipa pamaso pa Mulungu. Ndipo chifukwa cha tchimo loopsya losalekeza la anthuwo, Mulungu analikananso mfuko la Yuda kuti likhale Ufumu Wake. Nthawiyi, nkuti Zedekiya akulamulira mfuko la Yudalo. Iwo anagonjetsedwa ndi a Babulo (2 Mafumu 25). Anakhala

ku Babulo kwa zaka 70 ndipo apa mpamene ena mwa ana a Israeli adabwerera kudziko lawo motsogozedwa ndi Ezra kuphatikizapo Nehemiya. Iwo sanathenso kulamulidwa ndi mfumu yawo-yawo ayi chifukwa kenaka adalamulidwa ndi a Babulo, a Helene (Greeks) ndi Aroma. Yesu adabadwa m'nthawi ya ulamuliro wa Aroma. Popeza ana a Israeli anakana Yesu, Aroma anathira nkondo m'chaka cha A.D. 70 ndipo a Israeli onse anamwazidwa kukhala m'dziko lonse lapansi. Anamwazika ku mayiko amene iwo sankadziwako chibadwire chawo. Mzaka 100 zapitazo, ana a Israeli anayamba kubwerera kwao ku Israeli (onani Mpatuko wa chitatu).

Ezekieli 21:25-27 analosera kale zakutha kwa Ufumu wa Mulungu kudzera mfuko la Israeli motere: ***“Ndipo iwe wolasidwa oyipa kalonga wa Israeli (mwachitsanzo, Zedekiya) amene lafika tsiku lako, nthawi ya mphulupulu yotsiriza; atero Ambuye Yehova, Chotsa chilemba, bvula korona, Ufumu sudzakhhalanso momwemo, kweza chopepuka, chepsya chokwezeka. Ndidzagubuduza gubuduza gubuduza Ufumu uno, sudzakhhalanso kufikira akadza Iye Mwini chiweruzo; ndipo ndidzaupereka kwa Iye”*** Onani kuti manunsu a m'mabuku a aneneri ambiri amalosera kwambiri za kutha kwa Ufumu wa Mulungu (Hoseya 10:3; Maliro 5:16; Yereimiya 14:21; Danieli 8:12-14).

Kugubuduzika katatu kwa Ezekieli 21:25-27 kunkalosera za kuthiridwa nkondo kwa ana a Israeli ndi mfumu Nebukadinezara wa ku Babulo. Munthu ophunzira weni weni wa Baibulo, adzaona yekha kuti pali kufanana pakati pa m'mene Ufumu wa Mulungu ndi mfumu yake (Zedekiya) zinalandirira m'nyozo mofanana. Kutha kwa ufumu wa Zedekiya kudayimiranso kutha kwa Ufumu wa Mulungu umenense udaali wa ana a Israeli (onani Phunziro 5.2).

Mwaichi, Ufumu wa Mulungu unatha pamene Ufumu wa ana a Israeli unathanso: ***“..ndidzabwezera ...ndi kuleketsa ufumu wa nyumba ya Israeli”*** (Hoseya 1:4). Kutha kwa Ufumu umenewu kukuonetsa kuti udzabwezeretsedwanso. ***“Ndipo Ambuye Mulungu adzampatsa Iye mpando wa Chimfumu... ndipo Iye adzachita Ufumu pa banja la Yakobo kunthawi zonse, ndipo ufumu wake sudzatha;”*** (Luka 1:32,33) pamene Khristu adzabweranso. Ichi ndicho chikonzero cha Mulungu pamene adzakwaniritse lonjezo lake

lobweretsanso Ufumu Wake wa Mulungu. Onaninso kuti Ufumuwo udzakhazikitsidwanso pokhapokha Yesu adzabwerenso osati lero ayi.

KUBWEZEREDWA KWA UFUMU WA ISRAELI (UFUMU WA MULUNGU)

Uwu ndi mutu wodziwika kwambiri m'mabuku onse a aneneri m'Chipangano Chakale pofotokozera za kubwezeretsa kwa Ufumu wa Mulungu kwa ana a Israeli (Israeli wa uzimu) pamene Mesiya adzabweranso padziko lapansi pano. Akuphunzira ake a Yesu anawuzidwanso zambiri pankhani imeneyi: ***“Pamenepo iwowa, atasonkhana pamodzi, anamfunsa Iye, nanena, Ambuye kodi panthawi ino mubwezera Ufumu kwa Israeli?”*** mwachitsanzo, ‘kodi Ezekieli 21:27 tsopano akwaniritsidwa?’ Yesu anawayankha ponena kuti nthawi yeni yeni yakubweranso kwa Iye sadzadziwa ayi, ngakhale kuti Angelo kenaka adawatsimikizira kuti Yesu adzabweranso posachedwapa kudzaweruza komanso kudzakhala ndi anthu padziko lonse lapansi (Machitidwe 1:6-11).

Kubwezeredwa kwa Ufumu wa Mulungu / Israeli kotero, kudzachitika pamene Khristu adzabweranso panso pano. M'njira imeneyi, Petro analalikira kuti Mulungu adzatumiza ***“ndipo atume amene anayikidwa kwa inu, Khristu Yesu.... amene thambo la kumwamba liyenera kumlandira*** (mwachitsanzo, ayenera akhale kumeneko) ***kufikira nthawi za kukozanso zinthu zonse, zimene Mulungu analankhula za izo mkamwa mwa aneneri ake oyera chiyambire”*** (Machitidwe 3:20,21). Kubweranso kwa Khristu kudzabweretsanso kukhazikika kwachiwiri kwa Ufumu wa Mulungu omwensho ndi Ufumu wa ana a Israeli (koma apa adzakhala Israeli Oyera) umene kalelo udaali Ufumu wa ana a Israeli. Kubwereranso kwa Ufumu wa Mulungu ndiyo mfundo yaikulu yomwe yakhala ikulalikidwa ndi aneneri osiyana siyana kuchokera kalelo:-

- ***“M'chisomo chomwecho ndi mwa chifundo, Ufumuwo udzakhazikitsidwa; ndipo*** (Yesu Khristu) ***adzampatsa mpando wachifumu wa Davide atate wake*** (pamene adzabweranso [Luka 1:32,33]) ***nadzaweruza, nadzafunitsa chiweruzo....kuchita chirungamo”*** (Yesaya 16:5).
- ***“Tsiku lomwelo ndidzautsa msasa wa Davide*** (i.e. Ufumu wa Davide wa Luka 1:32,33) ***udagwawo, ndi kukonzanso zopasuka zake; ndipo ndidzautsa zogumuka zake, ndikumanga monga masiku a kalelo”***

- (Amosi 9:2). Onani kuti mau omalizirawo akufotokozeratu mwa chimvekere za kubweranso kwa Ufumu wa Israeli / Mulungu.
- *“Ana awonso adzakhala (ana a Israeli) monga kale ndipo msonkhano wao udzakhazikika pamaso panga, ndipo ndidzalanga onse amene akupsyinja iwo (panopa)”* (Yeremiya 30:20).
 - *“Ndipo Yehova adzalandira cholowa chake Yuda, ...naadzasankhanso Yerusalemu”* (Zekariya 2:12), Kudzaupanga Mzinda umenewu kuti udzakhale likulu la Ufumu Wake wadziko lonse lapansi (cp. Masalmo 48:2; Yesaya 2:2-4).
 - *“Ndipo ndidzabweza undende wa Yuda ndi wa Israeli, ndipo ndidzamangitsa mudzi wao, monga poyamba paja...mudzamvekanso mau akukondwa ndi mau akusekera,...Pakuti ndidzabweza undende wa dziko monga poyamba...mudzakhalanso (mu Yerusalemu) mokhalamo abusa ogonetsa zoweta zawo...zoweta zidzapitanso pansu pa manja a iye amene aziwerenga”* (Yeremiya 33:7-13).

Kubwezeranso kwachiwiri Ufumuwo (Mzinda wa Yerusalemu) pano kudzapangitsa kuti Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwe ndipo ichi ndicho **“Chiyembekezo cha Israeli”** chimene ifenso ngati **“Israeli wa Uzimu”** tiyenera kuyembekezeranso.

5.4 UFUMU WA MULUNGU MTSOGOLOMO

M’Phunziro 3.1 ndi 3.3 mgawo lomwe lino, tapindula koposa pakumva mfundo zofunikira kwambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu, momwe Ufumuwo udzafikire komanso momwe udzakhaliye padziko lapansi lino. Taona kuti Mulungu analonjeza kwa Abrahamu kuti adzamudalitsa; Aroma 4:13 akuonjezeranso kuti dziko lonse lapansi lidzadalitsidwa, ndinso kuti lidzapatsidwa kwa mwana (mbeu ya) wa Abrahamu mwachitsanzo, kudzera mwa Khristu Yesu.

Fanizo la Danieli 2 likufotokozerwa momwe Khristu adzabwerera ngati kamwala kakang'ono, ndipo kuti Ufumu wa Mulungu udzakwanira padziko lonse lapansi (cp. Masalmo 72:8). Izi zikutanthauza kuti Ufumu wa Mulungu sudzangokhazikitsidwa ku Yerusalemu kokha, kapena m'dziko la Israeli lokha komanso malo amodzi okha monga ena amanenera ayi; ngakhale kuti tikudziwa malo amenewa ndi amene adzakhale malo oyambirira kukwaniritsa pa kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulunguwo.

Onse amene akutsata Yesu panopa ndi amene adzakhale “mafumu ndi ansebe” ndipo “tidzachita ufumu” (tidzalamulira) padziko (Chibvumbulutso 5:10). Tidzalamuliradi malo osiyana siyana monga m'makulidwe ena mizinda khumi, komanso ena isanu, (Luka 19:17). Khristu adzatigawira Ufamuliro Wake padziko lino lapansi (Chibvumbulutso 2:27; 2 Timoteo 2:12). ***“Taonani mfumu idzalamulira m'chilungamo, ndi akalonga*** (Yesu ndi okhulupirira onse) ***adzalamulira m'chiweruzo*** (Yesaya 32:1; Masalmo 45:16).

Khristu adzalamulira “kunthawi zonse” pa chimpando chachimfumu cha Davide chimene chidzakhazikitsidwanso (Luka 1:32,33), mwachitsanzo, adzakhala pa chimpando cheni cheni cha Davide ndi malo eni eni a ufamuliro wake amene adaali mu Yerusalemu. Monga tamva kuti Khristu adzalamulira kuchokera mu Mzinda wa Yerusalemu lomwe lidzakhale likulu la Ufumu wa Mulungu, kumeneku ndi kumene kudzamangidwe kachisi wa Yehova (Ezekieli 40-48). Pamene anthu onse m'dziko lonse lapansi azidzalemekeza Mulungu (Mlaliki 1:11), kachisi ameneyu ndi amene adzakoke anthu onse a m'mayikowo kuti azikapemphera mkachisiyu. Mayiko a mitundu yonse ***“adzabwera chaka ndi chaka kulambira mfumu Yehova wa makamu, ndi kusunga madyerero a misasa***” yomwe yazungulira kachisi wa Yerusalemu (Zekariya 14:16).

Ulendo umenewu wa pa chaka umene anthu azidzapita ku Yerusalemu, unalosedwa ndi Yesaya 2:2,3:- ***“Ndipo padzakhala masiku otsiriza, kuti phiri*** (Ufumu wake – Danieli 2:35,44) ***la nyumba ya Yehova lidzakhazikika pa nsonga ya mapiri*** (mwachitsanzo, Ufumu wa Mulungu udzakwezedwa pamwamba pa mafumu a anthu).....***ndi mitundu yonse idzasonkhana kumeneko. Ndipo anthu ambiri adzamka, naati, Tiyezi tikwere kumka ku phiri la Yehova, ku nyumba ya Mulungu*** (Kachisi) ***wa Yakobo; ndipo Iye***

adzatiphunzitsa za njira zake,...chifukwa m'Ziyoni mudzatuluka chilamulo, ndi mau a Yehova kuchokera m'Yerusalemu.” Mfundo imeneyi ikutipatsa chithunzi thunzi cha koyambirira kwa Ufumu umenewu wa Mulungu pamene anthu azidzayesetsa kufalitsa Uthenga Wabwino kuti Khristu wayamba ulamuliro Wake; Koteru, anthu azidzapitadi ku phiri la kachisi wa Mulungu Yehovayo kukadzionera okha Ufumuwo, umene pang’ono pang’ono udzafalikira m’dziko lonse lapansi. Apa tiri ndi chithunzi thunzi chabwino tsopano cha m’mene akhristu a lero ayenera kulambira Yehova wa makamu ndinso kamasulidwe komanso kamvetsedwe koyenera ka Mau a Mulungu ponena za Ufumuwo.

Chinthu choopsya kwambiri masiku ano ndi chakuti anthu ambiri amapembedza Mulungu pa zifukwa za ndale, ena kudzisangalatsa, kukumana kapena kukacheza ndi anzawo, pamene ena chili ngati chikhalidwe cha mfuko lawo, enaso chifukwa chokhudzidwa ndi zimene anaona kwa anzawo panthawi ya maliro, ndinso ena kungonthunthumira chabe kapena tinene kuti kungotengeka ndi zochitika kumaloko. Chifukwa cha zimenezi, kumapezeka kuti iwo samatha kudziwa zambiri zokhudza Yehova ngati Atate wao koteru, Mulungu alibe naye chidwi. Mu Ufumu wa Mulungu, anthu osankhidwawo adzakhala okhawo amene ali ozindikira ndipo adzakhala ndi chidwi ndi Mulungu wao. Iwo adzakhala onthunthumira komanso kulaka laka kumudziwitsitsa Mbuye wao pophatikiza m’mene akumudziwira lero lino. Monga tawerenga, anthu adzakangamira Yehova mpaka kuyenda dziko lonse lapansi ndi cholinga chofuna kukawona kachisi wa Mulungu m’Yerusalemu watsopano pofuna kuzindikira kwathunthu za Yehova Mlengi wawoyo.

M’malo mwa chisokonezo ndi kusoweka chilungamo kwa masiku ano m’mayiko, zomwe zinadza chifukwa cha chikonzero cha chiweruzo cha munthu cha bodza ndi ulamuliro wake wonyenga, m’malo mwake kudzabwera panthawiyo, *“Chilamulo ndi Mau a Ambuye”* omwe adzalalikidwe ndi Khristu kuchokera mu Yerusalemu. *“M’mayiko onse amitundu adzasonkhanitsidwa kumeneku,”* Chiphunzitso chimenechi chikuonetseratu poyera kuti sipadzakhalanso kukangana ndi kutetana, chifukwa munthu aliyense nthawiyo adzalaka lakadi kudziwa za Yehova Mpulumutsi wake. Koteru, kulimbana pakati pa mayiko kudzatha.

Mayiko onse kukasonkhana ku Yerusalemu ndi chimodzi modzi chithunzi chimenechi chokhala ndi zolinga zimodzi, motero tinene kuti tikuchipezanso powerenga pa Yesaya 60:5, pomwe a Yuda **“adzasonkhanitsidwe pamodzi”** kuphatikizapo amitundu omwe onse akapembedze Mulungu mu Yerusalemu. Apa zikugwirizana kwathunthu ndi ulosi wa Zekariya wa Ufumuwo pa Zekariya 8:20-23:-

“Kudzachitikanso kuti mitundu ya anthu, ndi okhalamo m’midzi yambiri adzafika, ndi okhala m’udzi umodzi adzamuka ku mudzi wina, ndi kuti tiyeni msanga” (mg. Cp. Zekariya 14:16 ‘chaka ndi chaka) **kukapeza Yehova ndi kufuna funa Yehova wa makamu; ndimuka inenso. Inde, mitundu yambiri ya anthu, ndi amitundu amphamvu adzadza kufuna funa Yehova wa makamu m’Yerusalemu, ndi kupeza Yehova. ...amuna khumi adzagwira iwo amanenendwe onse a amitundu, inde adzagwira mkawo wa munthu ali m’Yuda ndi kuti, ‘Tidzamuka nanu, pakuti tamva kuti Mulungu ali ndi inu.’**

Apa tikuoneratu kuti a Yuda ndiwo akutenga mbali yaikulu yautsogoleri pa mutu umenewu wa Ufumu wa Mulungu; **“Mutu osati m’chira”** wa mayiko ayi chifukwa cha kulapa ndi kumvera kwao (Deuteronomo 28:13); Mwaichi, chikhulupiriro cha a Yuda m’cholinga cha Mulungu pa chipulumutso cha munthu, chidzaloledwa kwa yense waife padziko lapansi. Kusazindikira izi ngakhale ziri zofunika pakati pathu akhristu a lero kotero, kudzathera pamenepa, pamene tidzalake lake kumudziwa Iye. Anthu kotero, adzakhala akukambirana zoterezi moteronso, iwo adzathe kuwuzwa a Yuda kuti **“tamva kuti Mulungu Yehova ali nanu.”** Tione tsopano kuti kudzatheka kuthetsa mkwiyo pokambirana za Yehova chifukwa anthu adzakhala ndi chidwi pa Chiuta wao zimene ziri zosiyana koposa ndi kutetana kumene kukuchitika leroku!

Chifukwa chakudzipereka kwa aliyense pozindikira zambiri za Namalenga wathu, sizidzakhala zachilendo kuwona kuti Khristu **“adzaweruzwa pakati pa akunja, adzadzudzula mitundu yambiri ya anthu; ndipo iwo adzasula malupanga awo akhale zolimira, ndi nthungo** (mikondo/spear?) **zawo zikhale anangwape** (prunninghooks?); **mtundu sudzanyamula lupanga kumenyana ndi mtundu wina, ndipo sadzaphunziranso nkhondo”** (Yesaya 2:4). Ulamuliro wa Khristu ndi chiweruzo cha chilungamo chake zonse zidzathetsa nkhondo ndi

malo onse ankhondo amene tikuwaona lerowa kuti adzakhale malo osiririka, amalimidwe, ndipo mabalakisi onse adzathera pomwepo. ***“M’masiku ake olungama adzatuluka”*** (Masalmo 72:7 – note translation error). Chipembedzo kotero, chidzakwezedwa pamwamba ndipo onse opembedza adzalemekezeka chifukwa cha chikondi, chifundo ndi chiweruzo choonadi cha Mulungu. Taganizirani izi mogwirizana ndi zimene zikuchitika lero pakati pathu – kudzikweza, kudzikonda ndi kudzikundikira komanso kudzitamandira ndi zina zotero!

Ngati munthu adzafika posula malupanga nkuwasandutsa zida zolimira, zikuonetseratu kuti iwo paokha adzasintha khalidwe la uchigawenga, la nkhondo, nkukhala anthu okonda mtendere pokondanso kulima m’mina yawo ndipo izi sizingadzachitike kumwamba ayi. Chifukwa cha tchimo la Adamu, nthaka inatembereredwa (Genesis 3:17-19) kotero, munthu panopa ayenera kukheta thukuta kuti nthakayo ibale zabwino. Mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo, ***“m’dzikomo mudzakhala zinthu (zakumunda) zochuluka pamwamba pa mapiri (nthaka yoguga); zipatso (zokolola) zakale zidzati waa, ngati za ku Lebanoni”*** (Masalmo 72:16). ***“...wolima adzapambana wokolola, woponda mphesa adzapambana wofesa, ndi mapiri adzakhetsa vinyo wokoma”*** (Amosi 9:13), izi ndi zomwe zidzachitike pa nthawiyo ndipo chonde chambiri chidzakuta malo onse kuphatikizapo mapiri omwe adaali malo osabala monga mwatemberero la m’unda wa Edeni.

Chitukuko chachikulu cha malimidwe chidzafikira anthu onse. Ulosi wa aneneri ukuonetsa kuti padzakhala chitukuko cha ulimi chimene chidzatipatse kudzidalira pamoyo wathu:-

“Koma adzakhala munthu yense patsinde pa mpesa wake, ndi patsinde pa mkuyu wake; ndipo sipadzakhala wakuwaopsya,” (Mika 4:4).

Kudzidalira pa zonse kudzathandiza kuthetsa mabvuto a ntchito ndi umphawi zimene zilipo lero’zi. Kugwira ntchito yonse yomwe imalemeretsa anthu ena monga zikukhalira masiku ano, zidzatha.

“Ndipo iwo adzamanga nyumba ndi kukhalamo; ndipo iwo adzaoka minda ya mphesa, ndi kudya zipatso zake. Iwo sadzamanga, ndi wina kukhalamo; iwo sadzaoka, ndi wina kudya; pakuti monga masiku a

mtengo adzakhala masiku a anthu anga; ndi malo osankhidwa anga adzasangalala nthawi zambiri za manja ao. Iwo sadzagwira ntchito mwachabe, pena kubalira tsoka; pakuti iwo ndiwo mbeu ya odalitsidwa a Yehova, ndi obadwa ao adzakhala pamodzi ndi iwo.” (Yesaya 65:21-23).

Pa Yesaya 35:1-7 tikuwerengapo za ulosi wapamwamba wonena za nthaka yopanda chonde imene idzasinthidwa ndi mphamvu ya Mulungu kukhala nthaka ya chonde, ulosi umenewunso ukutitsimikizira kuti Mulungu yemweyo adzabweretsadi chisangalalo chachikulu pakati pa anthu onse chifukwa cha ‘umwana alilenji’ umenewu m’nthaka yobereketsa zokolola zambirizo. **“Chipululu ndi malo owuma** (ndiwo malo kapena tinene kuti nthaka imene) **adzakondwa; ndipo dziko loti see lidzasangalala; ndi kuphuka ngati duwa, lidzaphuka mochuluka ndi kusangalala ngakhale kukondwa ndi kuyimba...pakuti m’chipululu madzi adzatuluka, ndi mitsinje m’dziko lonse kuti see.”** Ngakhale mkwiyo wa nyama udzatha **“...mbulu ndi mwana wa nkhosa idzadyera limodzi,”** ndipo ana adzasewera ndi njoka (Yesaya 65:25; 11:6-8).

M’njira imeneyi, temberero lomwe linayikidwa m’manda wa Edeni uja lidzathera pamenepa. Chibvumbulutso 20:2,3 akukamba m’chiphiphiritso za m’dierekezi (ntchito ndi zotsatira zake za tchimo) kuti **“adzamangidwa”** naatsekeredwa m’ndende kwa zaka chikwi. Umoyo wa munthu udzakhala wautali kotero, ngati munthu afa pakadzatha zaka zana limodzi, adzakambidwa kuti wafa akadali mwana wamng’ono (Yesaya 65:20). Akazi sadzakhala ndi ululu pamene adzabala mwana (Yesaya 65:23). **“Pamenepo maso a khungu adzatsegulidwa, ndi makutu a ogontha adzatsegulidwa. Pamenepo wopunduka adzatumphu ngati nswala ndi lirime la wosalankhula lidzayimba”** (Yesaya 35:5,6). Zonsezi zidzachitika chifukwa anthu adzakhala ndi mphatso za Mzimu panthawi imeneyo (mphatso za mtengo wapatali - A Hebrai 6:5).

Tiyenera kudziwa kuti Ufumu wa Mulungu suli ngati m’mene zimakhallira kunyanja anthu akakhala pa tchuthi kukapuma nakasangalala ayi. Cholinga cha Ufumu wa Mulungu ndicho kukwaniritsa kuti munthu payekha ayenera kulemekeza ndi kudziwa Mulungu kotero, dziko lonse lapansi lidzaze ndi ulemmerero wa Mulungu Yehova monga **“madzi adzaza nyanja”** (Habakuk 2:14).

Ichi ndicho cholinga cheni cheni cha Yehova – “*..koma ndithu, pali ine, dziko lonse lapansi lidzadzazidwa ndi ulemerero wa Yehova,*” (Nume 14:21). Ulemerero kwa Mulungu nkutanthauza kuti anthu onse okhala panso pano adzayenera kukhutitsidwa, kulambira, kupempherera ndinso kutengera chitsanzo ndi zinthu zonse zimene Iye Mulungu Mwini amachita nthawi zonse; Chifukwa chakuti dziko lapansi lidzachita ichi, Mulungu adzalolanso kuti onse apindule monga tawerenga kale ndi kuti ichi chidzakhala chithunzi thunzi cha munthu aliyense. Kotero, “*..Koma ofatsa adzalandira dziko lapansi (mu Ufumu wa Mulungu): Nadzakondwera nao mtendere wochuluka* (kukhutitsidwa ndi mtendere wa chipembedzo choyenera)” (Masalmo 37:11; Mateyu 5:6).

Kukhala ndi moyo wosatha mu Ufumu wa Mulungu imakhala ngati nyambo yokoma yokopera anthu kuti akhale ndi chidwi kotero, atembukire ku chi khristu masiku ano ngakhale kuti chikhristu cha anthu ambiri panopa n’chosayenera. Komabe, kukhala ndi moyo wosatha m’nthawi irinkudzayo mu Ufumu wake wa Mulungu, kudzayenera kuti Yehova Mulungu wathu adzalemekezeke, ichi ndicho chikakhala cholinga chathu cheni cheni. Palibe kanthu kuti tikhoza kukhala nthawi yaitali bwanji titabatizidwa kale podikira Yesu, koma tikalola kuti ndi chinthu choyenera ife kuchita, tidzayenera kukhutitsidwa nacho chikonzero cha Mulungu chimenechi ndipo momwemo, tidzanthunthumira kukwaniritsa chikonzero chimenechi polemekeza Mulungu Yehovayo. Kwaine, zaka khumi munthu akumvera ndi kuchita chifuniro cha Mulungu chikhoza kukhala chinthu chonyaditsa komanso chopindulitsa kwa munthuyo m’moyo uno pamene anthu ali otanganidwa ndi zam’dziko. Tikaganizira kuti chisangalalo chikubweracho n’chosatha mpaka muyaya wa muyaya, tiona kuti chingakhale chinthu cholimbitsa mtima kwambiri kukonzeratu tsogolo la moyo wathu. Kukhala mu Ufumu wa Mulungu choncho, chiyenera chikhale chilimbitso ndi chilako lako chathu nthawi zonse koterodi, tilolere kutaya ulemerero wa dziko lino m’moyo uno tiri nawo uno, komanso kuti tisiyedi zinthu zonse zimene tiri nazo ndi kuyika Khristu patsogolo pa zinthu zonse m’moyo uno. M’malo motaya nthawi kuganizira za m’mene tingapezere chuma cha moyo uno, Yesu akutilangiza kuti, “*..muthange mwafuna Ufumu wake ndi chilungamo chake ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwainu*” (Mateyu 6:30-34). Zonse zimene timaganiza ndi kuchita tsopano pa moyo uno

wa mdziko sizingafanane ndi chikwaniritso cha zonse zimene zidzachitike mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo monga m'chikonzero cha Iye.

Tiyeni tisankhe *“chirungamo ndi chiyero”* mwachitsanzo, kusankha ndinso kukonda chikhalidwe cha Umulungu kotero, tikakhale mu Ufumu wa Yehova Mulunguyo, popeza chirungamo chidzakhala ndipo chidzalemekezeka mu Ufumuwo; ndinso kuti popeza tafunitsitsa kusunga Chiyero cha Mulungu osati pongothawa imfa ayi, komanso kuti tikakhale nawo moyo wosatha m'chisangalalo cha muyaya mu Ufumu wa Mulungu.

Tikaonetsetsa, chiyembekezo cha Uthenga wa Ufumu wa Mulungu chikulalikiidwa m'malo osiyana siyana lerolino, komanso m'malalikiidwe osiyana siyananso; uwu ndiwo Uthenga Wabwino ngakhale kuti chifukwa chodzikhonda, anthu ambiri amawusanduliza Uthenga Wabwino uja pofuna kukwaniritsa zolinga zawo. Chikanakhala choyenera kulimbikitsa ulaliki weni weni wa choonadi umene umatsamiradi pa malembo oyera ngakhale kuti zoterezi lero zikusoweka. Nzowonekeratu kuti m'njira imeneyi ya chikondi cha Mulungu, anthu onse adzalimbikitsidwa kwambiri pamene adzakhale mu Ufumu wa Mulungu Wathu. Kotero, tinenetse kuti chikhale chilako lako cha aliyense waife padziko lapansi, kuphunziradi ndi kuzindikira, kukhulupirira, komanso kudzipereka ndi kulimbikira potenganso mbali pa ulaliki woonadi otere. Tiyeni timvere lamulo la Mulungu kuti tiyenera kubatizidwa moyenera monga mwachikonzero choyenera cha ubatizo weni weni wa tanthauzo. Tikatero, tidzakula mu uzimu komanso, tidzakhala okhwima mu nzeru za chikhulupiriro cheni cheni cha Uthenga Wabwino.

5.5 CHIRUMIKA

Tsopano tafika m'maphunziro athu a umoyo mu Ufumu wa Mulungu, ena akhoza kuona ngati kuti zakambidwazi ndi zoganiza munthu chabe. Tizindikire kwamphamvu kuti zokambirana zathu zikuchitika powunikirana zinthu zeni zeni

zimenedi zidalembedwa m’Baibulo. Mfundo zonse m’buku lino zafotokozedwa motsogozedwa ndi zolembedwa m’Baibulo pa mutu umene ukukambidwawo; kotero, n’chifukwa chake tikutsimikizira powerenga kuti munthu mu Ufumu wa Mulungu, azidzaberekana (Yesaya 65:23) ndiponso kuti adzafa (Yesaya 65:20). Si ife anthu wamba amene tikunena izi ayi, koma Baibulo loyera’lo limene ifedi tiyenera kulimvetsa bwino lomwe komanso kulikhulupirira. Anthu amenewa tikuwerenganso kuti ngakhale iwo adzakangamirabe m’kukangana, komabe Khristu adzawayanjanitsa (Yesaya 2:4); iwo adzayenera kugwira ntchito, kulima n’cholinga chakuti adzakhale ndi moyo wabwino ngakhale kuti izi zidzakhala zosabvuta kuzichita poyerekeza ndi m’mene zinthu ziriri lerolino. Chifukwa chosamvetsa bwino, ena akhoza kuona ngati kuti sizikugwirizana ndi malonjezo a moyo wosatha, komanso umoyo ndi uthunthu ofanana ndi Mulungu, kotero tidzafanane ndi angelo amene samakwatira ndi kuberekana (Luka 20:35,36). Baibulo silingadzitsutse koterodi, yankho lake liripo m’Baibulo lomwelo. Yankho lake ndilo kunena kuti gawo loyamba la Ufumu wa Mulungu lidzakhala kwa zaka chirumika chimodzi (zaka 1,000 [Chibvumbulutsu 20:2-7]). M’nthawi imeneyi, padzakhala magulu awiri a anthu padziko lapansi:-

1. Anthu Oyera – onse amene anatsata Yesu Khristu, naalola kutsogozedwa ndi Khristu’yo m’moyo wao onse kotero, panthawiyo, adzapatsidwa moyo wosatha pa Chimpando cha chiweruzo. Onani kuti ‘Oyera’ akutanthauza “munthu oyitanidwa ku chiyezo” ndipo ndimunthu okhulupirira choonadi.
2. Anthu wamba – amene adzathe kufa komanso panthawiyo adzakhala asanamvepo chilichonse chokamba za Uthenga Wabwino pamene Khristu Yesu adzabwerenso padziko lapansi – i.e. iwo amene analibe udindo wina uliwonse pa Chimpando wa chiweruzo.

Khristu akadzabweranso, anthu awiri adzakhala m’munda, m’modzi adzatengedwa (ku chiweruzo), ndipo winayo, “.....adzasiyidwa” (Luka 17:36) *kutanthauza kuti kulima kudzakhapobe*; ena onse amene “adzasiyidwe” adzakhala mgulu limeneri lachiwirilo.

Akadzangolandira chikhalidwe ndi maonekedwe a Umulungu pa Mpando wa chiweruzo, oyerawo, iwo saadzafanso komanso sadzabalana. Anthu amene akukambidwa mgulu lachiwiri’li kotero, adzakhala okhawa amene panthawi

yobwera Khristu Yesuyo adzakhale ndi moyo, koma adzakhale kuti adaalibe udindo wina uliwonse wakumva Uthenga Wabwino choncho, sanathe kukhala ndi mwayi wodziwa zofunikira pa chikonzero cha chipulumutso cha Mulungu. Mphatso ya kuyera ndi chilungamo idzakhala “..ndipo mudzawayesa iwo mafumu ndi nsembe: naadzalamulira padziko lapansi” (Chibvumbulutso 5:10). Mafumu amayenera kulamulira anthu; onse amene sanathe kudziwa Uthenga Wabwino panthawi yomwe Khristu adzabwerensoyo, adzayenera kusiyidwa kuti akhale ndi moyo kotero, adzalamulidwe ndi kuphunzitsidwa ndi anthu oyera mtima komanso olungama pamaso pa Mulungu amene adzakhaledi ataonekera kale pamaso pa Chimpano cha chiweruzo. Pokhala “mwa Khristu”, tidzagawanadi mphatso yake, imene ndiyo kulamulira dziko lapansi: “..Iye amene alalika, ndi iye amene asunga ntchito zanga, kufikira chitsiriziro, kwa iye ndidzapatsa ulamuliro wa pa amitundu; ndipo adzawalamulira ndi ndodo ya chitsulo...monga Inenso ndalandira kwa Atate wanga,” (Chibvumbulutso 2:26, 27).

Motero, fanizo la Khristu la ndalama khumi likugwirizana koposa ndi mfundo imeneyi: *akapolo okhulupirika aja anapatsidwa mphatso mogwirizana ndi ntchito zawo kuti ena athe kulamula mizinda khumi, ena isanu mu Ufumu wa Mulungu* (Luka 19:12-19). Njira za Mulungu sizidzadziwika msanga pamene Khristu adzakhala atangopatsidwa Ufumu wa Mulungu wa mu Mzinda wa Yerusalemu; N’chifukwa chake, anthu adzapita ku Yerusalemu kuti akapeze umboni ndi nzeru zokwanira zokhudza Mulungu wawo’yo (Yesaya 2:2,3). Kumbukaninso momwe phiri la Danieli 2:35,44 (imene likuyimira Ufumu wa Mulungu) linakulira mpaka kudzaza dziko lonse lapansi. Izi zikuonetsa kuti udzakhala udindo wa olungama onse kufalitsa Uthenga Wabwino wa Mulungu pa dziko lonse lapansilo choncho, ngakhalenso za Ufumu wakewo anthu akewo adzaufalita.

Pamene mfuko la ana a Israeli kalelo lidaali mu Ufumu wa Mulungu, udindo wa ansembe amenenso ankalamulira, udaali ophunzitsa anthu zambiri zokhudza Mau a Mulungu (Mlaliki 2:5-7; Ezara 7:10). Chifukwa cha cholinga chimenechi, ana a Israeli ankakhala ndi ansembewo m’matauni osiyana siyana m’dziko lonse la Israeli. Pamene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwanso

padziko lapansi, olungama onse adzavala udindo wa ansembe (Chibvumbulutso 5:10).

Ngati Khristu atabwera lero:

1. Onse amene adafa atazindikira kale Mau Oyera, adzawukitsidwa, ndipo pamodzi ndi onse ozindikira Mau Oyera amene adzakhala ndi moyo adzasonkhanitsidwa ku Mpando wa chiweruzo wa Khristu Yesu.
2. Onse amene adzapezeke ochimwa adzalangidwa ndi chilango cha imfa, ndipo onse olungama adzapatsidwa mphotho ya moyo wosatha. Mayiko ndi anthu amene amakana chiphunzitso choyenera cha Khristu, adzaweruzidwanso.
3. Olungama onse kotero, adzalamulira anthu onse amene adzakhale ndi moyo, koma sanathe kukhala ndi mwayi wozindikira Mau a Mulungu ndi Yehova wawo; Iwo adzaphunzitsidwa Mau a Uthenga Wabwino ndi olungamawo ngati “mafumu ndi ansembe” awo (Chibvumbulutso 5:10).
4. Ndondomeko imeneyi idzachitika mzaka 1,000 zoyambirira. M’nthawi imeneyi, anthu wamba adzamva Uthenga Wabwino choncho, iwo adzakhalsanso ndi udindo pamaso pa Mulungu. Anthu amenewa adzakhala ndi miyoyo yaitali komanso osangalala ndipo kenaka sadzatchedwanso anthu wamba.
5. Pakutha kwa chirumikachi, anthu ena adzayamba kuukira Khristu ndi olungama onse ndipo kuwukirako kudzazimitsidwa ndi Mulungu Mwini (Chibvumbulutso 20:5,8,9).
6. Ndipo pomaliza kweni kweni kwa zaka 1,000 ena onse amene m’nthawi ya chirumikayo adzawukitsidwe, adzaweruzidwa (Chibvumbulutso 20:11-15).
7. Osalungama onse m’chiweruzo chimenechi adzaonongedwa ku imfa yosatha, pamene olungama onse adzapatsidwa moyo wosatha kuti akhale pamodzi ndi ena aja omwe panthawiyi, adzakhala mafumu komanso ena adzachita unsembe.

Mwaichi, cholinga cheni cheni cha Mulungu polenga dziko lapansi tsopano chidzakwaniritsidwa. Dziko lino kotero, lidzadzazidwa ndi anthu olungama komanso a moyo wosatha. Dzina la Mulungu loti “Yahweh Elohimu” (lomwe limatanthauza kuti “Iye owululidwa mgulu la akulu onse”) lidzakwaniritsidwa

panthawi imeneyi. Kotero, tchimo ndi imfa sizidzaonekanso padziko lapansi; lonjezo lomwe lija lonena kuti mbeu ya njoka ija idzathudzulidwa mutu, lidzakwaniritsidwa pamenepa (Genesis 3:15). Kuyambira mkati kati mpaka nthawi yonse ya chirumika, Khristu adzakhala atalamulira “*kufikira atayika adani onse pansi pa mapazi ake. Mdani wotsiriza amene adzaphwasulidwa ndiye imfa...Ndipo pamene zonsezo zagonjetsedwa kwa Iye (Mulungu), pomwepo Mwana yemwe anagonjetsa adzamumvera Iye (Mulungu) amene anamugonjetsera zinthu zonse, kuti Mulungu akhale zonse mu zonse*” (1 Akorinto 15:25-28 [please note the Chichewa translation errors in this verse!])

Iyi ndiyo nthawi ya “*..chimaliziro, pamene (Khristu) adzapereka Ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate,*” (1 Akorinto 15:24). Nanga chidzachitika nchiyani pamene Mulungu adzakhale “*zonse mu zonse,*” izi sitinawuzidwe; zimene tikudziwa ndizo zakuti, tidzakhala ndi moyo wosatha, uthunthu ndi chikhaliidwe cha Mulungu ndiponso kuti tidzakhala mu umoyo wolemekeza komanso wosangalatsa nawo Mulungu. Tiona kuti ndi zosafunika kweni kweni kudziwa kuti chidzachitike n’chiyani ikadzatha nthawi ya chirumikayo.

Kuzindikira zonse zokhudza “*Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu*” ndi kofunikira kwambiri pa chipulumutso cha moyo wathu pakati pathu komanso kwa munthu wina aliyense amene awerenga zimenezi. Ife tikukupemphani kuti muwerengenso Phunziro lino ndipo chitani ichi mofatsa kotero kuti, mumvetse bwino pofufuza m’ndime zimene zapatsidwazo m’Baibulomo. Ngati mungakhale ndi mafunso ena aliwonse khalani omasuka kufunsa polembera ku ma adiresi ena onse amene apatsidwa m’buku lino.

Mulungu akufunitsitsa kuti ife tonse tikakhale mu Ufumu Wake, n’chifukwa chake, Iye analenga inu ndi ine ndipo kuti panali cholinga. Cholinga chake chonse ndicho kuti ife tonse tikakhale ndi mbali pa chikonzero chimenechi osati kungodziwa nkumalalikira za chilengedwe chake osachitapo kanthu ayi. Ubatizo ndi umene umatienereza ife kumalonjezano a Ufumu wa Mulungu umenewu. Tikudziwa kuti kwa anthu ena, nkobvuta kukhulupirira kuti ubatizo, kumvera pa kanthawi kochepe kwa Mulungu zingakhale ndi mbali pa mphatso ya moyo wosatha. Tiyeni tidziwe kuti chikhulupiriro chatu cholimba pa chikonzero cha Mulungu ndi chofunikira koposa. Ngakhale tikhale ndi zifukwa zotani pofuna

kunyozero Mau a Mulungu, palibe phindu lina lirilonse lomwe tingalipeze, koposa tibvomereze mayitanidwe a Mau ake.

“Ngati Mulungu ali ndi ife, adzatiletsa ndani? (note translation errors - Aroma 8:31)

“Pakuti ndiyesa kuti masauko a nyengo yatsopano sayenera kulinganizidwa ndi ulemerero umene udzaonetsedwa kwa ife” (Aroma 8:18).

“Pakuti chisautso chathu chopepuka cha kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakulu kulu ndi kosatha kwa ulemerero” (2 Akorinto 4:17).

MPATUKO 15: ZOONA ZENI ZENI ZA UFUMU WA MULUNGU

Zimene timawerenga pa nkhani yokhudza Ufumu wa Mulungu zopezeka m’Chipangano Chakale, zomwensho zidalembedwa ndi aneneri ndizimene a khristu a matcharitchi ambiri komanso otsatira awo samagwirizana nazo, amazikana. Ena amanenanso kuti mau oti ‘dziko lapansi’ ndi chiphiphiritso cha malo ena ake operekerako mphotho Kumwamba popeza dziko lino lapansi lidzakhala litaotchedwa.

Mongofotokozerapo zimenezi, tiyenera tizikhala odziwa kuti Baibulo ndi lomveka bwino palokha pozindikira kuti zinthu zonse zomwe zinalembedwazo mogwirizana mmitu yake, zidalembedwa mowuziridwa ndi mpweya wa Mulungu. Pokha pokha ngati ife tikuyika maganizo athu m’mitu yolembedwa kaleyo ndiye kuti tidzayamba kuona kusiyana pakati pa zimene zidalembedwazo ndi maganizo athuwo!. Ngati pali chiphiphiritso chimene chalembedwa pa mutu wa nkhani kapena buku lina, Baibulo limaneneratu zaizi; Mwachitsanzo, Buku la Chibvumbulutso ndime 1:1, lidafotokozeratu kuti ndicho *“chiphiphiritso, (kapena tinene kuti) chizindikiro chaonetsedwa kwa Yohane”* (onani kuti Baibulo la Chichewa silinafotokozere bwino izi m’ndime yoyambayi). Palonso njira yomwe mabuku ena a m’Baibulo amaonetsera pofuna kuti ife tizindikire kuti nkhaniyo yalembedwa m’chiphiphiritso mwachitsanzo, tikawerenga za

“dziko lapansi limene lidzachita dzandi dzandi, ngati munthu woledzera” (Yesaya 24:20), nzowonekeratu kuti apa tiyenera kuwerenga ngati chiphiphiritso. Mosiyana ndi izi, malo amene amakamba za Ufumu wa Mulungu sanafotokozedwe mwa chiphiphiritso ayi, chifukwa timawerenga m’ndime zambiri zimenenso sizidalembedwe m’chiphiphiritso.

Zikuonekeratu kuti chifukwa cha kuchepa kwa chikhulupiriro kwa munthu kuti izi zingadzachitikedi pa dziko lapansi, anthu tsopano anayamba kupeka nthano zawo zokhudza Ufumu wa Mulungu ndi mitu ina ya m’Baibulo kuti zonsezi zigwirizane ndi maganizo awo. Anthu owatsatira nawo samaonanso bvuto lina lirilonse popeza kwaiwo samafuna kudzibvuta pomawerenga Baibulo paokha kuti amvetse, amakhala alibe chidwi cheni cheni chimene chingawathandize kuti athe kumasulira paokha Mau a Chiyero’wa. Pano ife sitinganenenso za njira ina iriyonse ya Ufumu wa Mulungu kuti ungakhale kumwamba monga ena amanenera chifukwa palibe umboni wina uliwonse onena za kumwamba m’Baibulo. Ngati wina anganene kuti anthu opunduka adzaongoka, mzipululu mudzakhala chonde komwe kudzabala zokolola zambiri, zonse apa ndi ziphiphiritso kotero, sizikutanthawuza zeni zeni monga timagwiritsira ntchito mau amenewa ayi; tiyenera kudzifunsa kuti *“ndi ziphiphiritso zoyimira chiyani?”* Ndime zimenezi zonse zikukamba za m’mene Ufumu wa Mulungu udzakhali ndipo ndinkhani yodziwikiratu m’Baibulo. Kotero, tinene pano poyera kuti ngati sitikudziwa kuti ziphiphiritso zimenezi zikutanthauzanji, ndiye kuti sitikudziwanso zambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu choncho, sitidzakhala ndi mbali ina iriyonse pa chipulumutso.

Popitiriza, tikhoza kunenanso kuti potengera zimene taphunzira, taona kuti Mulungu ali ndi cholinga chosatha ndi munthu panso pano osati kumwamba ayi; Iye sangaphwasule dziko lapansi limenenso analonjeza kwa mbeu ya Abrahamu kuti idzakhalamo kunthawi zonse zosatha ayi. Mwaichi, tiyenera kutsimikizira kuti zimene Mulungu analonjeza panthawi’yi, ndi zeni zeni sinkhambakamwa chabe ayi.

Ndime ziri m’munzizi zikutsimikizira zonse zimene zalembedwa pamwambazi:-

- *“Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwachabe; Iye analiumba akhalemo*

anthu;” (Yesaya 45:18). Kulengedwa kwa dziko lapansi kukhoza kukhala kwachabe ngati Mulungu adzaliwononge; Koma, mosiyana ndi izi, ncholinga cha Mulungu kuti anthu amene adzalandire moyo wosatha adzakhale m’dzikomo.

- “*..dziko lingokhalabe masiku onse*” (Mlaliki 1:4 (silidzatha ayi)).
- “*Anazikhazikanso (nyenyezi ndi dzuwa) kunthawi za nthawi; Anazipatsa chilamulo chosatumphika*” (Masalmo 148:6).

Nthawi ya chirumika chimodzi (1,000) monga timawerenga pa Chibvumbulutso 20:4 ndi nthawi yeni yeni kotero, tikalola ndi kubvomereza kuti nthawi imeneyi ndiyo nthawi yeni yeni, tidzaona kuti zikutipatsa chithunzi thunzi cheni cheni cha Ufumu wa Mulungu ndi cholinga chake. Komanso, tidzazindikira zimene aneneri analemba kalelo. Onaninso kuti ngakhale buku lonse la Chibvumbulutso tiyenera kuliwerenga ngati buku la ziphiphiritso. Tikudziwa kuti si mau onse amene ndi ophiphiritso ayi komabe mbali yaikulu ya ndime zambiri m’buku limeneri ndi ziphiphiritso chifukwa ndime yoyamba m’buku limeneri ikufotokozeratu motero. Tionanso kuti mau ambiri amakamba za ndime zina zomwe ziripo kale m’mabuku a m’Baibulo.

Tisayiwalenso kuti m’chiphiphiritso momwemo, timawerenga za chiphiphiritso cha ulamuliro wa chaka cha “chikwi” pa Ahebri 4:4-9 chomwe chakambidwa ngati tsiku la Sabata – tsiku lopuma. Apa Paulo akunena za tsiku limodzi m’chiphiphiritso kuti ndi chimodzi mwa zinthu zambiri zomwe zidzachitike m’chaka cha “chikwi” chimenechi. Kumbukaninso kuti 2 Petro 3:8 akunena kuti “*tsiku limodzi likhala kwa Ambuye ngati zaka chikwi, ndi zaka chikwi ngati tsiku limodzi*”. Choncho, Paulo akufotokoza za chaka cha chikwi pamene anakamba za tsiku limeneri la chipumulo. Kotero, akunena kuti pakatha zaka zikwi 6, cholinga cha Mulungu chikuphunzitsidwabe padziko lino lapansi, padzafika nthawi ya mpumulo ya chaka “chikwi chimodzi-1000”. Pakadali pano, tatha kale zikwi zambiri kotero, zikhoza kutheka kuti tiri m’nthawi yomaliza ya chikwi cha chisanu ndi chimodzi. Ndipo Paulo akunena kuti chikwi cha Sabata (zomwe ndi zaka 1,000), Mulungu adzakwaniritsa zambiri mwa zinthu zina zimene analonjeza kwa anthu ake. Mwachitsanzo, Uthenga Wabwino udzalalikidwa kwa anthu amene adzakhale asanamvepo Mau a Mulungu chibadwire.

Tikaganizira za chilengedwe m’Baibulo, tikhozanso kuzindikira kuti dziko lapansi ndi zinthu zonse zidalengedwa kwa zaka 6,000 (mwachitsanzo, masiku 6 akuyimira zaka 6,000 ngati tsiku limodzi lingakhale zaka 1,000 kwa Ambuye [2 Petro 3:8]). Ndipo ngati chilengedwe chinachitika mzaka za 4,000 B.C. monga ena amanenera, ndiye kuti chaka cha 2,000 A.D. kapena kupitirirapo pang’ono chikhoza kukhala chomaliza. Izi zikutanthawuza kuti nthawi yatha; Khristu athadi kubwera nthawi ina iriyonse panopa. Choncho, tiyenera kuyesetsa kukwanitsa chikonzekero chathu kuti Khristu akamabwera atipeze tiri ojera ndipo kuti tikaonekere pamaso pake. Tiyeni tonse tiyembekezere chaka chimenechi molimbitsidwa ndi Mau ake.

MPATUKO 16: MBIRI YAKALE YA ANA A ISREALI MWACHIDULE

ABRAHAMU anayitanidwa ndi Mulungu kuti achoke mu Mzinda wa Ur kwao kwa ma Kedushi; nakakhala m’Yuda woyamba. Mulungu Yehova anamulonjeza iye kuti adzamupatsa dziko la Kanani kudzera mwa mbeu yake. Iye anamwalira osalandirabe lonjezo lake la dziko la Kanani. Iye sanalandirebe mphatso za lonjezo la Mulungulo.

ISAKE: Abrahamu adaali okonzeka ndi chikhulupiriro chake kupereka mwana wake yekhayo paguwa ngati nsembe yopsereza kwa Mulungu. Chifukwa cha chikhulupiriro chimenechi, Mulungu anaonjezera malonjezano ake kwa Abrahamu. Chilakolako cha Isake kuti adzafe akusungabe ndinso kumvera malamulo a abambo wake Abrahamu, zinaonetsa chiphiphiritso cha Khristu. Isake adaayimira Yesu Khristu. Malonjezano a kwa Abrahamu aja koteru, anabwerezedwa komanso kuonjezereka kwa Isake pamwamba pa malonjezano akalewo (Genesis 26:3-5).

YAKOBO: Adaali mwana wa Isake. Malonjezano aja anatsimikizidwanso kwa iye. Iye anali ndi ana 12 (khumi ndi awiri) – ndipo wamkulu kwambiri woyamba

anali Reubeni, pamene wamng'ono kwa onsewo ndiponso womaliza adaali Benjamini. Yosefe anali mwana wake wopatulika, wokondeka komanso wapamtima.

YOSEFE: Akadali mwana wamng'ono, adalota maloto kawiri amene adalozera kuti tsiku lina adzalamulira abale ake aja. Abale akewo ankamuchitira nsanje kotero, adamugulitsa ku ukapolo kwa Aigupto. Kumeneko iye anakhala mtsogoleri wamkulu wokonza za kasungidwe ka chimanga cha dziko lonse lapansi. Chimanga chimenechi chinali chodzagwiritsa ntchito nthawi ya njala yoopsa yomwe ikanadzafika zaka zisanu ndi ziwiri zakutsogoloko kuchokera pa nthawi ya maloto'yo. Nthawi ya njala itakwana, dela lonse la Kanani linakhudzidwa ndipo Yakobo ndi ana ake onse omwe anali nawo ku Kananiko, anafika ku Aigupto kukakhala ndi Yosefe. Yakobo ndi ana ake ena amene anabadwa ku Aigupto'ko, ankakhala m'chigawo cha Gosheni. Itafa mfumu Farao, mfumu imene idalowa m'malo mwake inawada koposa ana a Israeli. Ana onse obadwa kumene ankaphedwa pa nthawi imeneyi n'cholinga chakuti ana a Israeli asachulukane.

MOSE: Anabadwa m'nthawi yobvutayo pamene ana onse amuna a mfuko la ana a Israeli ankaphedwa, mwaichi, adabisidwa m'chitete cha bango akadali khanda, kenaka, anapezeka akuyandama pamadzi ndipo amene anampeza ndi mwana wa mkazi woyamba wa Farao. Mose akadali m'nyamata, adapha m'modzi wa ana a Aigupto amene ankamenya munthu wina wa mfuko la Israeli. Kenaka Mose anathawira ku dziko la ku Midiyani kumene anakhalako zaka 40 akuweta nyama za Yetero. Mulungu anamuonekera m'chilangali chamoto chimene chinkayaka pa tsamba la mtengo koma tsambalo silinkapsya. Iye anauzidwa kuti apite kudzikolo la Aigupto, kwa mfumu Farao kukapulumsa ana a Israeli. Mose anaonetsa masilamusi osiyana siyana motsogozedwa ndi Mulungu kuti Farao ndi gulu lake amvetse kutidi iye anatumidwadi ndi Mulungu. Ngakhale zinali choncho, Farao sanatekeseke ndipo kotero, sanalole kuti ana a Israeli achoke mu Aigupto moteronso, Mulungu anatumiza miliri khumi yosiyana siyana monga ya achule, ntchentche, zilonda zobuka zokha, mdima, matalala; Ndipo komaliza, imfa ya ana oyamba amuna a anthu onse a mwa Aigupto inawafikira. Ana a Israeli anapulumutsidwa chifukwa adayenera kupha mwana wa nkhusa nkupaka magazi ake pamphuthu za nyumba zawo. Izi tikhoza kuona kuti zinkaloserana za

kutsogolo pomwe mwazi wa Yesu Khristu udzapulumutsa onse okhulupirira kuimfa. Ndipo madyerero amene adachitika nthawiyo adaatchedwa *Paskha*.

EKSODO: Ana a Israeli kenaka analoledwa kuchoka ku Aigupto. Iwo anayenda motsogozedwa ndi m'ngelo wa Mulungu mu mtambo woyima njoo masana ndi moto woyima njoo usiku. A nkondo a Farao anawalondola ana a Israeli mpaka kufikira m'nyanja yofiira. Madzi panyanjayo anagawanikana pakati modabwitsa anthu onse pamene ana a Israeli ankawoloka m'nyanja yofiirayo. Kenaka anayambanso kuyenda mwamphamvu pamene a nkondo a Aigupto aja anafika pakati kati pa nyanja ija kotero, anamira onse.

Ana a Israeli pamenepa anatha kuyenda bwino tsopano popanda chiopsyeyo china chirichonse podzera njira yozungulira m'chipululu pa ulendo wao wopita ku dziko la malonjezano. Mulungu anawayendetsa njira imeneyi pokana kuti angangoyamba kumenyana ndi Afilisiti ngati akanadzera njira ya chidule molunjika dziko la Kanani, m'njira imeneyi, akanabwereranso ku Aigupto chifukwa cha mantha ndi nkondoyo. Izi zikanapangitsa kuti aganizirenso kubwerera kukakhalanso ku Aigupto kumene kunaali dziko la machimo ambiri pamaso pa Mulungu. Yehova anawapatsa iwo madzi ochokera m'thantwe la paphiri lotchedwa Horebu, ndi mkate womwe unkatchedwa '*mana*' m'mawa uliwonse. Atafika pa phiri la *Sinai*, Mulungu anawapatsa malamulo khumi ndinso malamulo a Mose. Apa ndi pamenenso Yehova Mulungu anawafotokozera kuti iwo ndiwo *Ufumu wa Mulungu* ndipo kuti mfumu ya ufumu umenewu ndiye Mulungu. Mwaichi, a Israeli onse ankalamulidwa ndi Mulungu kuti ndithu ayenera kupembedza Mulungu wao m'modzi yekhayo. Kotero, Yehova Chiuta wa makamu anawauza a Israeli kuti amange chihema chapadera chotchedwa *kachisi* ndi *likasa* mopembedzeramo Yehova. Iwo anapatsidwanso wansembe wamkulu ndi ansembe ena amene ankapsyereza nsembe pa guwa la moto kwa Mulungu Namalenga. Tiona kuti zonsezi zimene zinkachitika m'malo amenewa a nsembe, zinkalosera nthawi ndi ntchito ya Khristu Yesu kutsogoloko pamene Khristu akanadzabadwa, naperekedwa ngati nsembe yopsyereza pamene anapachikidwa pamtanda ndipo Iye anafa imfa yonyozeka ngati nyama.

DZIKO LAMALONJEZANO: Dziko la Kanani linayandikira. A kachenjede a azondi khumi ndi awiri anatumizidwa kuti akachite uzondi m'dzikolo ndipo khumi mwa azondiwo, anabwerera ndi uthenga oti n'kobvuta kulanda dzikolo chifukwa chakuti anthu ake adaali amphamvu kwambiri. Awiri mwa azondi aja amene sanabwerere msanga, Yoswa ndi Karebu atafika, anakamba zookha zookha kuti atha kulanda dziko la malonjezano'lo ngati anthu onsewo angakhale ndi chikhulupiriro chawo mwa Chiuta wao. Chifukwa chakuti ana a Israeli adakhulupirira kwambiri maganizidwe azondi khumi aja, adayenda yenda m'chipululu kwa zaka makumi anayi; mpaka pamene ana a Israeli onse amene anachokera ku Aigupto ali ndi zaka makumi awiri adafa chifukwa chosowa chikhulupiriro mwa Mulungu wawo.

YOSWA: Ndi amene analowa m'malo mwa Mose kulumulira ana a Israeli kupita ku dziko la malonjezano la Kanani. Mzinda woyamba kuwugonjetsa unaali wa Yeriko, kumene ankakhala Rahabe, kenaka analanda mzinda wa Ai. Atakhazikika mu Kanani, ankalamulidwa ndi *Oweruza*, amene analamuliradi Israeli motsatana tsatana ngakhale kuti Mfumu Yawo yeni yeni idaali Chiuta Namalenga. Ena mwa Oweruza'wa adali Gideoni, Yefita ndi Samsoni. Onse analanditsapo Israeli kuchokera m'manja mwa adani awo, pamene adalapa ku machimo pamaso pa Mulungu wao. Onani kuti mbiri ya ana a Israeli iri ndi zitsanzo zambiri za mabvuto amene ankawapeza chifukwa chosamvera Mulungu; monga kulangidwa kudzera m'nkhondo zochuluka, kugonjetsedwa kenaka nkulapa, kuchimwiranso Mulungu ndi zina zotero. Oweruza omalizira m'nthawi imeneyi adaali Samueli. Nyengo yomweyi, Israeli anakana Mulungu kuti ndiyo Mfumu Yawo ndipo anawonetsera ichi pamene anafunitsitsa kukhala ndi mfumu monga mayiko ozungulira iwo analiri.

MFUMU: Mfumu yao yoyamba idali Sauli amene poyambapo, adayamba bwino bwino, koma kenaka, anakhala munthu woyipa kwambiri; Iye sanasungenso malamulo a Mulungu ndipo anazunza Davide. Atafa Sauli, Davide anakhala mfumu ya Israeli kulowa m'malo mwake. Davide koteru, anali m'modzi mwamafumu abwino zedi a Israeli. Moteronso, Mulungu anapangana naye Davide, namulonjeza malonjezano akulu. Atafa Davide, mwana wake Solomoni analamulira Israeli. Iyenso adaayamba bwino koma kenaka, anasandulika naachita zoyipa chifukwa cha akazi ambiri amitundu mitundu amene iye

anawakwatira. Ndipo iye atafa, ufumuwo unagawikana pawiri- mafuko khumi anapanga ufumu wa Israeli molamulidwa ndi Yeroboamu; pamene mafuko awiri otsalawo a Yuda ndi Benjamini adatchedwa Ufumu wa Yuda ndipo ndi amene ankalamulidwa ndi Rehobiamu mwana wake wa Solomoni.

Ufumu wa Israeli (mafuko khumi aja) siunali ndi mafumu abwino. Ankawukira Chiuta pafupi pafupi. Mulungu adawatumizira aneneri ambiri amene anawapempha kuti asiye machimo awo koma sizinatheke. Chifukwa chaichi, a Asuri anathira nkhondo yawo pa ana a Israeli nawagonjetsa, ndipo anawatengera kundende nakakhala kudziko la a Assuri. Kenaka, ana a Israeli anamwazikana ndipo anapezeka ali padziko lonse lapansi.

Ufumu wa mfuko la Yuda (mafuko awiri ophatikizana aja) adaali ndi mafumu abwino ochepa monga Asa ndi Hezekiya komabe, iwonso sanamvere Mulungu. Anthu a ku Babulo anatumizidwa ndi Mulungu kukathira nkhondo mafuko awiri'wa, ndipo atagonjetsedwa, anatengedwanso ukapolo kumka m'dziko la Babulo kumene anakhalako kwa zaka makumi asanu ndi awiri. Kuchokera pamene, sanakhalenso ndi mfumu yamtundu wina ulionse yochokera mfuko lawo. Zaka 70 zitatha, ena mwa iwo adaabwerera ku Israeli motsogoleredwa ndi Ezara, Nehemiya, Yoswa (wansembe wamkulu) ndi Zerubabelo Gavanalayo. A Israeli'wa koyambirirako anaalamulidwa ndi dziko la Persia kenaka dziko la Greece ndipo komaliza analamulidwa ndi Aroma. Pamene Yesu Khristu ankabadwa, nkuti ali m'manja mwa Aroma. Chifukwa chakuti a Israeli anamukana Yesu Khristu, Chiuta, Mphambe anatumanso a Aroma kuti aphwasule Yerusalemu ndipo ichi chinali chaka cha 70 A.D., kotero, ana onse a Israeli anathamangitsidwa mdziko lawo la Israeli kachiwiri.

Posachedwapa, ana a Yuda anayambanso kubwerera kudziko lawo, moteronso, mpaka lero lino akubwererabe m'modzi m'modzi, kusonkhana kudziko lawo la Israeli, komwe kukukwaniritsadi ulosi osiyana siyana opezeka m'mabuku ambiri a aneneri m'Chipangano Chakale. Kuyambanso kwa mfuko la Israeli kukhalanso dziko loyima palokha; ichi kunali kutsimikiziranso kuti ndicho chizindikiro chimene chikutionetsa kuti Yesu Khristu ali pafupidi kubweranso padziko lino lapansi, kuti adzakhazikitse ufumu wa Israeli ngati Ufumu weni weni wa Mulungu.

PHUNZIRO 5: MAFUNSO

1. Ndi nthawi yanji mwanthawi zapatsidwa pansizi imene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwe?
 - (a) Ufumu wa Mulungu wakhala ukukhazikitsidwa
 - (b) Pamene Khristu adzabwerenso padziko lapansi
 - (c) Pa tsiku la Pentekoste m'chirumika choyamba
 - (d) M'mitima mwa okhulupirira one pamene amatembenuka mtima wawo.
2. Kodi Ufumu wa Mulungu unayamba wakhalapo kale? Ngati ndi choncho, Unalipo mwanjira yotani?
3. Nanga Ufumu wa Mulungu'wo ngati unalipo unatha nthawi iti?
4. Kodi chaka cha chirumika ndi chiyani?
 - (a) Ndicho chisomo chopezeka m'mitima mwathu
 - (b) Ulamuliro wa zaka 1,000 wa okhulupirira kumwamba
 - (c) Ulamuliro wa zaka 1,000 wa satana padziko lino lapansi
 - (d) Zaka 1,000 zoyamba mu Ufumu wa Mulungu ulinkudzawo panso pano.
5. Kodi Ufumuwo udzakhala wotani?
6. Kodi okhulupirira alero lino azidzachita chiyani mu Ufumu wa Mulungu mzaka 1,000 zoyambazo?
 - (a) Adzatsogolera anthu ena amene anali asanamve Mau a Mulungu kotero azidzathanso kufa chifukwa iwo adzakhala asanazindikire Mau'wo.
 - (b) Adzalamulira kumwamba
 - (c) Sitikudziwa
 - (d) Adzakhala ndi moyo kudziko linalo
7. Kodi Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu udalalikidwapo kale?
 - (a) M'Chipangano Chatsopano chokha
 - (b) Ndi Yesu komanso ndi akuphunzira ake okha
 - (c) Mzipangano zonse Chakale ndinso Chatsopano
 - (d) M'Chipangano Chakale chokha.

Mukayankha mafunso'wa chonde tumizani ku imodzi mwa ma adiresi mwapatsidwa m'mapeji oyambirira a buku lino.

PHUNZIRO 6

**MULUNGU KOMANSO
CHAKWAYIPA**

6.1 MULUNGU KOMANSO CHAKWAYIPA

A khristu ambiri mogwirizana ndi azipembedzo zina zambiri amakhulupirira kuti kuli chinthu china chamoyo ndi champhamvu chotchchedwa m'dierekezi kapenanso Satana chimene chimayambitsa tchimo ndi mabvuto onse amene ali m'dziko lino lapansi; Iwo amanena kuti chilombo chimenechi chimatichimwitsa tsiku ndi tsiku m'moyo uno. Baibulo limatiphunzitsa momveka bwino kuti Chiuta ndi wamphamvu zochuluka. Taphunzira m'Phunziro 1.4 kuti Angelo saachimwa. Ngati ife lero tikutsimikizadi ndipo tikhulupirira m'choonadi kuti Baibulo ndiwo Mau a Mulungu, komanso kuti ife timakhulupirira zonse zimene zidalembedwa m'menemo, tiona kuti zoonadi sizingatheke ndipo moteronso kuti sizingakhale zoonadi pangakhale chinthu china monga satama chimene chili chilombo champhamvu zambiri, chotsutsana ndi Mulungu wathu Wamphamvuyo ayi! Ngati tingakhulupirire zimenezi, ndiye kuti tikukayikira Ungwiro ndi Mphamvu zosaneneka za Mulungu komanso Ukulu wake wa Namalenga Chisumphu wathuyo. Mfundo imeneyi ndi yofunika kwambiri kuyimvetsa bwino kotero, nkoyenera kuzindikira mve mve mve pa matanthawuzo a mau ambiri m'Baibulo okhudza mfundo ya mdierekezi ndi satana ngati momwe Baibulo lidalembera pachiyambipo m'malo motenga zimene munthu amanena. Timawerenga pa A Hebri 2:14 kuti Yesu Khristu anaphwanya m'dierekezi ndi imfa yake ya pamtanda paja; choncho, pokha pokha titakhala ndi chizindikiro chabwino ndinso kumvetsetsa kokwanira matanthawuzo a mau amenewa mchilankhulo choyambiriracho, tidzathanso kudziwa ndikuzindikira bwino tanthawuzo leni leni m'ndime zimenezi ndi matanthawuzo ake pa ntchito ya Yesu Khristu ndinso uthunthu wa Khristu'yo.

Mdziko lonse lapansi, maka maka kwa anthu amene amati ndiwo akhristu, ambiri amakhulupirira kuti zabwino zonse zimachokera kwa Mulungu ndipo kuti zoyipa zonse zimachokera kwa mdierekezi kapena tinene kuti kwa Satana. Maganizidwe ngati amenewa siachilendo ayi; komanso simaganizo amene amapezeka mwa akhristu okha ayi. Anthu a ku Babulo mwachitsanzo, ankakhulupirira kuti pali milungu iwiri, mulungu wabwino komanso wakuwala, ndi mulungu woyipa komanso wa mdima, kotero, kuti milungu yonseyi inkatha kuphana. Koresi (Cyrus) mfumu yaikulu ya ku Persia

inakhulupiriranso zimenezi. Choncho, Yehova Mulungu anamulankhula “...*Ine ndiri Yehova, ndipo palibe winanso; popanda Ine palibe Mulungu; ndidzakumanga m’chiuno ngakhale sunandidziwa; kuti anthu akadziwe kuchokera kumatulukiro a dzuwa ndi kumadzulo, kuti palibe wina popanda Ine; Ine ndine Yehova, palibe winanso. Ine ndilenga kuyera ndi mdima; Ine ndilenga mtendere ndi choyipa* (N.I.V. linamasulira kuti kuopsya), *Ine ndine Yehova wochita zinthu zonsezi*” (Yesaya 45:5-7). Tawerenga kuti Mulungu ndi amene analenga chabwino ndi choyipa, mwachitsanzo, zoopsya zonse adalenga ndi Mulungu ndipo amazidziwa, nazibweretsanso kwaife; Iye Yehova amachita zonsezi, analenga zabwino komanso zoyipa, ndipo amazibweretsanso kwaife ndi Iye Yehova Mwini! Pano tiona kuti pali kusiyana pakati pa ‘choyipa’ ndi ‘tchimo’. Tchimo linabwera padziko lapansi chifukwa cha munthu amene analakwira Mulungu pochita zinthu zosiyana ndi zolembedwa m’chilamulo cha Mulungu’yo (Aroma 5:12).

Mulungu akumuuzza Koresi ndi anthu onse a ku Babulo *kuti “palibe winanso pamwamba pa Ine Yehova”*. Liwu la m’chi Hebri “el” limene linatanthawuzidwa kuti “**Mulungu**” limapereka chithunzi thunzi cha tanthawuzo la “**mphamvu**” kapenanso kuti “**kuchokera mmphamvu/mnyonga**”. Mulungu akunena kuti palibe kwina kulikonse kumene tingapezeco mphamvu koposa kwa Iye Chiuta. Chifukwa cha chimenechi, mkhristu weni weni amene amakhulupiriradi Mulungu, sangalolere mfundo yoti pali chinthu chinanso cha mphamvu pamwamba pa Mulungu; Yehova amene iye amamudziwa kuti ndi Wamphamvu zochulukadi kuposa wina aliyense kapena tinene kuti kuposa china chirichonse! Kotero, okhulupirira otereyu amadziwadi kuti kudziko kuno kulibe chinthu china chirichonse cha mphamvu chotchedwa satana, mdierekezi kapena tinenenso kuti *mzimu woyipa* monga alaliki ena amanenera. Tidziwa kuti Wamphamvu ndiye Mulungu yekha basi.

MULUNGU: ANALENGA ZOOPSYA

M’Baibulo muli zitsanzo zambiri zimene zimaonetsa kuti zoyipa zina ndi zina amabweretsa kapenanso tinene kuti anabweretsa ndi Mulungu Yehova. Amosi 3:6 akunena kuti ngati mu mzinda muli zoyipa, Mulungu ndi amene amachita zonsezi. Mwachitsanzo, anthu akamanena kuti ku mzinda wina kudali chibvomezi chachikulu, ambiri amanena kuti mdierekezi ndi amene anakonza ndipo kuti wabweretsa mabvuto amenewa ndi satana yemweyo. Mkhristu weni

weni wokhulupirira amayenera kudziwa kuti ndi Yehova amene amabweretsa zonsezi mwachikonzero chake monga tawerenga kale pamwambapa. Mika 1:12 akunenetsa kuti “...*popeza choyipa chatsika kwa Yehova kumka ku chipata cha Yerusalemu.*”. M’Buku la Yobu, timawerenga kuti Yobu anali olungama koma anapezeka kuti zinthu zake zonse zinatha. Buku limeneri limatiphunzitsa kuti zoyipa za m’oyo uno sizingafanane ndi zotsatira za chikhulupirira chimene timakhala nacho; Kapenanso tinene kuti ziyenera kugwirizana ndi kusakhulupirira kwathu pamaso pa Mulungu. Tikhozanso kunena kuti munthu sangayesedwe mopitirira m’mene iye angakwaniritsire m’chipiriro chake pamayesero amene amubwererawo. N’chifukwa chake, Yobu anazindikira izi ponena kuti “*Yehova anapatsa, Yehova watenga, lidalitsike dzina lake*” (Yobu 1:21). Iye sakunena kuti “***Yehova anapatsa ndipo Satana watenga***” ayi! Moteronso, Yobu akuchitiranso ndemanga mkazi wake: “***Ha! Tidzalandira zokoma kwa Mulungu kodi, osalandiranso zoyipa?***” (Yobu 2:10). Ndipo komaliza kwa buku limeneri, anzake a Yobu aja anamupepa naziziritsa mtima wake kuti ukhale m’ malo mwake chifukwa cha zowawa anazipezazo. Mwaichinso, anamulimbitsa mtima kuti asadandaule ndipo anamthokoza “...*pa zoyipa zonse Yehova anamfikitsirazi*” (Yobu 42:11 cp.19:21; 8:4). Kotero, pa zimenezi, tidziwa kuti mabvuto ndi zoyipa zonse zimachokera kwa Mulungu popeza Iye ndi amene amalolanso kuti zonsezi zizitionekera m’miyoyo yathu.

“*Pakuti iye amene Ambuye amkonda amlanga, Namkwapula mwana aliyense amlandira...koma chitatha, chipereka chipatso cha mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa nacho, ndicho cha chilungamo*” (A Hebri 12:6-11; Miyambo 3:11,12), izi zikuonetsa kuti mayesero amene timalandira kuchokera kwa Mulungu, amatitsogolera mkukula kwa chilongosoko ndi choonadi cha moyo wathu wa chikhristu. Tiona kuti mazindikiridwe otere akugwirizana ndi Mau a Yehova monga tawerenga; zimenezi ziri zosiyani kwambiri ndi m’mene anthu ena amanenera. Motero, sizoonza kunena kuti satana kapena mdierekezi ndiye amatichimwitsa ayi. Komanso sizoonza kuti zoopsya ngakhale mabvuto amene timawapeza amabweretsa kwaife ndi mdierekezi kapena kuti satana ayi, izi ndi zosiyana koposa ndi zimene Baibulo limanena. Tidziwe kuti sitiyenera kukhulupirira mfundo zonse ziwiri, chifukwa tiona kuti imodzi mwa mfundo ziwirizi sizikupezeka pena paliponse m’Baibulo ngakhale kuti a khristu a m’matcharitchi ena ambiri amalimbikira kulalikira kolimba pa mfundo zimenezi. Kotero, tionenso kuti zoyipa zonse analengadi ndi Mulungu ndipo

amabweretsa zonsezi kwaife ndi Yehova Mulungu monga tawerenga kale pamwambapa m'Baibulo. Mfundo imeneyi tingayipeze m'malo ambiri m'Baibulo monga timawerenga nthawi ndi nthawi. Ndime zina zimene akhristu oterewa samamvetsa zimawasokoneza iwo eni chifukwa amaganizira kwambiri zomwe iwowo amafuna kuti ziyenera kukhalira m'chikonzero cha chipulumutso m'maganizo mwao osati monga Mulungu Mwini anakonzera ayi. Choncho, zimamvetsadi chisoni kwa munthu amene akuzindikira ulalikiwu momveka bwino nadziwa koma nasankha dala kusokonekera mmamasuliridwe osiyana ndi momwe Baibulo likunenera. Chitsanzo china tiona pamene tiwerenga za kuperekedwa kwa munthu, *"kumpereka ...kwa satana, kuti liwonongeke thupi, 'kuti mzimu upulumutsidwe' mtsiku la Ambuye Yesu"* kapena kuti *"...ndawapereka kwa satana kuti aphunzire kusalankhula zamwano"* (1 Akorinto 5:5; 1 Timoteo 1:20). Ngati satana ndi chinthu china chobweretsa zoyipa pakati pa anthu, chifukwa chiyani satana m'ndime zimenezi akukambidwa kuti akuchita zinthu zabwino kwa anthu operekedwawo? Yankho lake apa tingati kweni kweni, n'chifukwa chakuti mtsutso wa zinthu, kapena kuti satana kapenanso tinene kuti nthawi ya umoyo wobvuta, zonse zimabweretsa chilimbitso pakati pa akhristu amene akupezana ndi zinthu zimenezi. N'chilimbitso chachikulu kwa akhristu oterewa chimene chirinso chothandiza kwambiri mkukula kwao, pamoyo wao wa chikhulupiriro champhamvu komanso pamaso pa Mulungu wao.

Tikamvetsa kuti choyipa chiri chonse chimachokera kwa Mulungu monga tawerenga m'Baibulo, tidzatha kupempha kwa Mulunguyo kuti atithandize, natichotsera zoyipa ndi mabvuto amene Iye watibweretsera'wo. Ngati Iye sangatichotsere zobvutazi, tiyenera kuzindikira kuti pali cholinga maka maka mwina pofuna kutichenjeza kapena kutilimbitsanso m'chikhulupiriro. Mwaichi, ngati ife timakhulupirira kuti satana kapena mdierekezi alipodi, ndipo kuti mabvuto athu amabweretsa ndi iyeyu, tionadi kuti kudzakhala kobvuta kwaife kukakhala ndi chikhulupiriro cheni cheni mwa Mulungu Wamphamvuyo kuti tikamupempha, angatithandize m'mabvuto athu omwe akubwera ndi satana. Choncho, ngati timakhulupirira kuti pali chinthu china chotchchedwa satana kapenanso kuti mdierekezi chimene chimatichimwitsa ndinso kutipatsa mabvuto onse amene tili nawo lero'wa, ndiye kuti kudzakhala kobvuta kuti mabvuto amenewa adzathe padziko lapansi; ndipo kuti zidzakhala zobvutanso kuti mfundo za m'Baibulo zigwirizane bwino monga zinalembedwera. Kupunduka, matenda, imfa yadzidzi kapena zoopsya

zina zonse zimaoneka ngati tachita tsoka chabe pamene mwina ndi nthawi kuti yatikwanira kotero izi zitionekera chomwechi. Ngati mdierekezi ndi chinthu champhamvu, m'ngelo wochimwa, tingati tikubvomereza kuti adzakhaladi wamphamvu zochuluka zedi kuposa mphamvu zathu zimene tiri nazo lero'zi (zimene amatipatsa ndi Yehova wamphamvu zonse) kotero, tiona ngati sitidzathadi kumugonjetsa koma kuti kudzakhala kumangozunzika m'dzanja lake. Ife amene timawerenga mau a Mulungu mozindikira komanso ndi chidwi chachikulu, chilako lako chathu chidzatilimbisa poona ndi kubvomereza kuti Mulungu ndi amene amabweretsadi zonse ndipo kuti tikamupempha kuti atichotsere zoyipa'zi, adzatithandiza chifukwa amadziwa bwino magwero a zinthu zonsezi. Motero, tionanso kuti amene akonda Mulungu *“zinthu zonse (m'moyo wao) zithandizana kuwachitira ubwino”* kwa okhulupirira onse (Aroma 8:28). Choncho, ife siife **“odala”** nthawi zonse mu umoyo wathu.

CHIYAMBI CHA TCHIMO

Nkofunika kudziwa komanso kutsimikizira kuti tchimo limayamba m'maganizo a m'mitima mwathu. Limakhala bvuto lathu kuti timachimwa osati chifukwa cha chinthu china chirichonse monga satana ayi. Nzoonadi kuti tikhoza kumanena zambiri pokhulupirira kuti ife timachimwa osati chifukwa cha bvuto lathu ayi koma chifukwa chakuti chinthu china ngati satana, chimatichimwitsa. Nthawi zambiri, anthu akachimwa, samalola kuti iwo ndi amene alakwira Mulungu ayi; Koma m'malo mwake amanena kuti mdierekezi ndi amene analowa m'mitima mwao nawachimwitsa, izi zikuonetsa kuti ife sitifuna kukhala ndi udindo pamoyo wathu; tinganenenso kuti tikutanthauwuza kuti ife sitingachimwe popanda satana. Tizindikire kotero, kuti tchimo lililonse limene tachita, Mulungu amaona ife kuti ndi amene tiri ndi udindo pa tchimo limenelo koteronso, tidzaweruzidwa pa zotsatira za tchimo limene'lo.

Tiyenera kukumbukira koteronso kuti *“mphotho ya tchimo ndiyo imfa”* (Aroma 6:23); *tchimo lititsogoza ife ku imfa.* Ngati siife amene timachimwa, ndiye kuti Mulungu ayenera kulanga satana mdierekezi: Chifukwa ndi amene amatipatsa tchimo lomwe mphotho yake ndiyo imfa. Kotero, ife sityenera kulandira chilango popeza sitimachimwa mwakufuna kwathu ayi. Tikaonetsetsa, tizindikiradi kuti siziyenera kukhala choncho chifukwa munthu akachimwa, amachita izi pofuna kudzisangalatsa osati pofuna kusangalatsa satana ayi. Tionenso kuti Mulungu anatichenjeza kuti tidzalangidwa ngati sitimvera Iye, Yehova sanati ngati satana samvera Iye ayi, koma ngati munthu

(amene amachimwa) sangamvere Mulungu Yehova! *Sananenedi kuti ngati Satana atichimwitsa ayi koma kuti ngati ife (eni) tichimwa.* Pamene timanena kuti pali chinthu china chamoyo ndi champhamvu, chimene chimatichimwitsa osati ife kuchimwa patokha mwa zilako lako zathu, sizoono ayi; Apa timangoonetsa kusabvomereza kwathu kuti sitili olungama. Ichi chimaonetsanso chitsanzo china poyera kutidi munthu akukana kwathunthu zonse zimene zinalembedwa m'Baibulo pa uthunthu wa Mulungu: kuti ali ochimwa pa chibadidwe.

“Kulibe kanthu kunja kwamunthu kakulowa mwa iye, kangathe kumdetsa: koma zinthu zakutuluka mwa munthu, ndizo zakumdetsa munthu...Chotuluka mwamunthu ndicho chidetsa munthu. Pakuti mkati mwache mwamitima ya anthu, mutuluka maganizo oyipa, za chiwerewere, zakuba, zakupha, za chigololo, masiro, zoyipa, chinyengo, chinyanso, diso loyipa, mwano, kudzikunza, kupusa: zoyipa izi zituluka mkati, nizidetsa munthu” (Marko 7:15-23).

Maganizo onena kuti mkati mwamitima mwathu mumalowa satana mdierekezi amene amatipangitsa kuti tizichimwa, tionadi kuti mfundo imeneyi sikugwirizana ndi chiphunzitso cha Yesu Khristu m'ndime imene tawerengayi. Yesu apa ananena zimene m'khristu aliyense ayenera kudziwa kuti ndizo zimabweretsa tchimo pakati pake; *'Kuti mkati mwamitima yathu mumatuluka zinthu zoyipa zimene zanenedwa m'ndime imeneyi'* ndi chimene Yesu anaona kuti n'chofunikira ife tichidziwe ndipo tiphunzitse ena onse amene sanakhale ndi mwayi wakudziwa chimenechi. N'chifukwa chake, nthawi yosefukira kwa madzi ija, Mulungu adaganiziranso kuti *“ndingaliro ya mtima wamunthu iri yoipa kuyambira pa unyamata wake”* (Genesis 8:21). Yakobo 1:14 akufotokozerana momwe mayesero amatifikira: *“...munthu aliyense (onani kuti nthawi zonse izi zikhoza kuchitika kwa munthu aliyense) ayasedwa pamene chilako lako chake cha iye mwini chimkomera, niichimnyenga”*. Iye timayesedwa ndi zolinga, zofuna, zilako lako ndi zokonda zathu zimene zimatikomera tikamachita tsiku ndi tsiku ndipo izi zonse n'zochokera mkati mwa mitima yathu osati kunja kwa ife eni wake ayi. *“Zichokera kuti nkhondo, zichokera kuti zolimbana mwainu?”* Yakobo akutifunsa, ***“Kodi sizichokera ku zikhumbo zanu zochita nkhondo mziwalo zanu?”*** (Yakobo 4:1). Aliyense waife ali ndi zinthu, komanso zilako lako zake zimene iye mwini (osati wina aliyense monga satana) amazikonda – zimenenso ndi mayesero ake a tsiku ndi tsiku. Choncho, zinthu zimene ziyenera kuchitika kwaiye yekha osati wina

kotero, akanakhala Satana, bwezi pano tiri ndi zilako lako (zinthu, zokonda ndi zofuna) zofanana m'miyoyo yathu. Mwaichi, aliyense ndi mdani wa iye yekha payekha chifukwa cha zochita zakezo.

Kalata ya Paulo kwa Aroma ikukamba motsindika za tchimo, magwero ake komanso m'mene tingagonjetsere tchimo. Muonanso kuti buku limeneri silikukambapo za mdierekezi kapena tinene kuti satana. Ndipo ponena za tchimo leni lenilo, Paulo sanafotokozepo kuti limachokera kwa satana kapena mdierekezi ayi. Mwanjira imeneyi, tiona kuti mdierekezi ndi liwu limene likupezeka m'Chipangano cha Chatsopano chokha. Pakanakhala kuti mdierekezi ndi chinthu champhamvu chimene chimatichimwitsa, m'Chipangano Chakale mukanalembedwanso zambiri zokhudza chinthu chimenechi kotero, anthu samamvetsetsa bwino pa za matanthauzo a mau amenewa. Koma chodabwitsa Chipangano Chakale sichinenapo chiri chonse za nkhanayi. Tikawerenga mabuku a Oweruza, kapena za mbili ya ana a Israeli m'chipululu, timamva kuti ana a Israeli ankachimwa pafupi pafupi. Koma Mulungu sanawadzudzulepo kuwachenjeza za chinthu china champhamvu chimene chingalowe m'mitima mwawo nkuwapangitsa kuti azichimwa ayi. M'malo mwake, Chiuta ankawalimbikitsa kuti iwo azisunga ndi kumvera malamulo komanso kusunga Mau ake kotero, asagwetsedwe mkuyesedwa chifukwa cha zofuna zathupi lawo, naachimwira Mulungu Yehova (Deuteronomo 27:9,10; Yoswa 22:5).

Paulo akulira choncho, *“Pakuti ndidziwa kuti mkati mwanga, (umu ndimo mthupi mwanga) simukhala chinthu chabwino, pakuti kufuna ndiri nako, koma kuchita chabwino sindikupeza. Pakuti chabwino chimene ndichifuna sindichita; koma choyipa chimene sindichifuna, chimenecho ndichita. Koma ngati ndichita chimene sindichifuna, sindinonso amene ndichita, koma utchimo wakukhalabe mkati mwanga ndiwo”* (Aroma 7:18-21). Tiona kuti Paulo anazindikira ichi. Iye sakudana ndi chinthu china ngati mdierekezi kuti ndicho chimene chimuchimwitsa ayi. Iye akunenetsadi kuti chilako lako chake, chimene chakhazikika mumtima mwake ndi chimene chimamuchimwitsa, ndipo kuti ichi ndicho gwero leni leni la utchimo wake. *“Sindine ndichita ichi koma tchimo limene liri mwaine, kotero ndipeza lamulo (mwaine), ndipo pamene ndifuna kuchita chabwino (monga mwa lamulolo!), choyipa chiripo kale mwaine (osati satana ayi!)”*. Choncho, pano Paulo akunenetsa kuti pamene iye afunitsitsa kuchita bwino monga mwa lamulo la Mulungu, mtsutso

ulipo kale mwayiye umene udana ndi chilungamo cha Mulungu Yehova mkati mwakemo. Aliyense apa ayenera kukhala ndi luntha ngati limeneri mchoonadi cheni cheni pozindikira payekha zoonadi zeni zeni za Mau ake a Mulungu.

Tizindikire kuti ngakhale a khritsu ake, akulu akulu okhwima mchoonadi ngati Paulo, sadasinthe mwanjira ina iriyonse mu uthunthu wao, koma kuti palibe nthawi yomwe iwo, angakhale Paulo akanalephera kuchimwa chifukwa chosinthika mu uzimu. Apa ndipamene chikhristu cheni cheni chimaonekera osati ngati momwe zimachitikira lero lino pakati pathu, pamene anzathu ena ngati a evanjeriko (evangelical) obadwanso mwatsopano amalalika. Choncho, alaliki otere akhoza kutanthauzira kuti ngakhale Paulo ndiye kuti sadali opulumutsidwa pamaso pa Mulungu chifukwa cha zimene iye ananena pa Aroma 7:15-21. Ndime zimenezi zikutionetseratu kuti anzathu amenewa angabvutike kwambiri kuti atifotokozere momveka bwino ndime zotere zizigwirizananso ndi chiphunzitso chawo. Davide, amenenso ali m'modzi owerengeka pa chikhulupiriro chake chozama kwa Mulungu motero, akuyikanso ndemanga yake pa Mau amenewa a tchimo makamaka pokhudza tchimo lake motere; *“Ndinakuzidwa m'tchimo, ndipo m'choyipa mayi anga anandibala”* (Masalmo 15:5 - please note the Chichewa translation error of the verse). Tiona kuti tchimo limene Davide ankanena pano linali tchimo limene iye ankachimwa pafupi pafupi komanso mowirikiza ngakhale iye sanali kufuna kutero.

Baibulo silibisa chirichonse pa za chibadidwe chathu mu uchimo wa munthu. Tonse tikangobvomereza zimenezi, sitingathe kupanganso kanthu kena kapena kukhala ndi chithunzi thunzi chinanso cha munthu amene sanachimwa chibadwire komanso za munthu amene sanaumirizidwepo kuchimwa chifukwa cha chilako lako chake ayi. Yeremiya 17:9 akunena kuti mtima wa munthu ndi wochimwa ndinso wachinyengo pa chibadidwe chake kotero, nthawi zina sitingamvetse zakukula kwa tchimo lake. Yesu Khristu pa Mateyu 7:11, ananeneratu mosabisa kuti umunthu wathu ndi wodetsedwa ndinso woyipa m'chikhalidwe. Mlaliki 9:3 akutsimikiziranso pa mfundo imeneyi *“...indetu mtimanso wa ana a anthu wadzala ndi choyipa”* (also note Chichewa translation error). Aefeso 4:18 akupereka chifukwa chimene munthu amakaniririra ndinso kuumirira kwa mitima yathu pa choyipa, maganizo athu oyipa mkati mwathu, ndizo zitilekanitsa ndi Mulungu Yehova. Mofanana ndi mfundo imeneyi, Agalatiya 5:19 akukambanso za machimo ngati *nchito za*

thupi (osati ntchito za satana); ndi thupi lathu lomwe umunthu wathu komanso mu uthunthu wathu ife timachimwa. Apa tizindikiradi kuti ndime zimenezi sizinanenepo kuti tchimo limabwera ndi mdierekezi ayi; tchimo linabwera mwaife m'chibadidwe chathu ndipo timakula nalo. Tikazindikira chabwino ndi choyipa powerenga Mau ake, tchimo ngati choyipa timatha kulisiya kapena kuti kuligonjetsa – kugonjetsa zilako lako zathu!

6.2 MDIEREKEZI NDI SATANA

Nthawi zambiri, mau amene adalembedwa mzilankhulo zoyambirira m'Baibulo samamasuliridwa m'chilankhulo china ayi (mwachitsanzo; mamoni liwu lomwe ndi la m'chi Aramaic – m'Chichewa ndilo anamasulira kuti ndi chuma.). Ndipo liwu loti “*satana*” ndi limodzi mwa mau amenewa, la chi Hebri limene liyenera kutanthauzidwa kuti “*mtsutsi*” pamene “*diabolosi*”, ndi liwu la m'chi Greek limenenso m'Chichewa lidamasuliridwa kuti ndi “*mdierekezi*”; koma tanthauzo leni leni lidayenera kukhala “*wonama, wabodza, wonenera bodza, wotsutsa mwabodza etc*”. Tikakhulupirira kuti ‘mdierekezi’ komanso kapena kuti ‘satana’ ndi chinthu china choyenda chokha mwamphamvu komanso choopsya pachokha, ndiye kuti tiyeneranso kuti tadziyikira maganizo athu pamwamba pa zimene Baibulo limanena. Tikakhala ndi maganizo amenewa pamene tikuwerenga za mau’wa m'Baibulo nthawi zonse, ndiye kuti tikulephera kuzindikira tanthawuzo leni leni la Baibulo kotero, ngakhale ndime zina sitidzatha kuzizindikira. Tiyenera tidziwe kuti Baibulo limagwiritsa ntchito mau a zining’a kotero tikamawerenga ena mwa mau a mtundu wotere, kungakhale kobvuta kumvetsa matanthauzo ake ngati sitidazame mzinging’a za mauwo. Mwaichi, Baibulo limanena zambiri za chinthu, mfumu kapena munthu, ndipo nthawi zina ngakhale ponena za angelo kapena Mulungu amene mchining’a kotero, kungatibvute kumvetsa kuti ndilo tanthauzo lonena za Mulungu kapena munthu. Ndipo malingana ndi m'mene Baibulo lidalembera za satana kapena mdierekezi, sangakhaledi chinthu china chapadera champhamvu chimene chimatichimwitsa pamene ife sitinafuno kutero monga ena amanenera ayi. Mfundo ya mdierekezi kapena tinene kuti

satana tikaganizira maulaliki a anthu ena, ikusiyanadi ndi zomwe Baibulo lomwe ndi Mau a Mulungu, limanena.

LIWU LONENA KUTI ‘SATANA’ M’BAIBULO

Tikawerenga 1 Mafumu 11:14, timva kuti *“Mulungu anamuutsira Solomoni mdani* (translation error – inayenera kukhala mtsutsi)” *“Hadadi mfumu ya Edomu.”* *“Ndipo Mulungu anamuwutsiranso mdani* (wotsutsa wina) *....Rezoni...anali mdani* (otsutsa wina) *.... kwa ana a Israeli”* (1 Mafumu 11:23,25). Pano, sizitanthauza kuti Mulungu anautsa chinthu china champhamvu zake, kapena chim’ngelo chonyasa kuti chikhale mdani, satana wa Solomoni ayi; Koma kuti anautsa anthu anzake, adani, ndipo maina a anthuwo atchulidwanso pa ndime zomwezi. Izi zikutiunikira kuti mau amenewa ali ndi matanthawuzo ake eni eni monga m’mene agwiritsidwa ntchito m’ndime zimenezi. Mateyu 16:22,23 akutipatsanso chitsanzo china chabwino pa mfundo yomweyi. Petro anayesetsa kukaniza Yesu.Khristu kuti asapite ku Yerusalemu pamene Yesuyo ananena kuti akafa pamtanda chifukwa cha tchimo la munthu. Yesu anacheuka nanena kwa Petro; *“Pita kumbuyo kwanga Satana iwe,(Petro) ndiwe chokhumudwitsa Ine; chifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu.”* Kotero, pano Petro akutchulidwa satana chifukwa anatsutsa Yesu. Malembo amenewa apa ndi achimvekere mopanda kuwonjezera kapena kupitiriza m’maganizo mwathu ponena monga ena amanenera kuti satana adalowa mumtima mwa Petro chifukwa Baibulo silikutero apa ayi. Kotero, m’maganizo mwa Yesu Khristu pamene pa ankanena Petro osati kwa chinthu china chotchchedwa Satana ayi. Ife sityenera kuyikaponso maganizo athu ofuna kukwaniritsa zikhumbo khumbo zathu pomanena kuti mdierekezi analowa m’maganizo mwa Petro ncholinga chofuna kumuchimwitsa ayi. Izi zidachitika chifukwa cha maganizidwe a umunthu wa Petro umene Khristu adadzera kuti maganizidwe oderera Mphamvu Za Mulungu ngati amenewa athe ngati ife tikhulupirira Khristu’yo. Tiona kuti Iye Yesu Khristu, sankakana maganizidwe athu opotokawo ayi, koma ankatipatsa mpata kuti tilankhule mopotoka chomwecho kenaka Iye atikonze *“Pita kumbuyo Satana...”* pamene ife tikhulupirira zonse zonena zachinthu china choopsya kotero kenaka titha kuzindikira kuti palibenso mphamvu ina iriyonse pa thambo lapansi yoponsa Mphamvu Ya Mulungu ndi mwa Yesu Khristu. Petro sanafune kuti Yesu akabvutike kotero chizindikiro cha moyo wosatha padziko lino lapansi chikhazikitsidwe ayi. Kotero, pokana zimenezi, ngakhale kuti zidalidi zoopsya, panthawiyo Petro adali Satana,

mtsutsi wa chikonzero cha Mulungu chomwe chinali chakuti Yesu Khristu ayenera kudzapachikidwa pamtanda. Mulungu anakonzanso kuti Satana (atsutsi monga Hadadi ndi Rezoni) kuti amutsutse Solomoni chifukwa cha machimo ake.

Tiona kotero kuti, chifukwa chakuti liwu loti Satana limatanthawuza kuti *“Mtsutsi”* kapena tinene kuti *“osagwirizana ndi zochita za anzako, zabwino kaya zoyipa”*; mau amenewa akugwiritsidwanso ntchito ngakhale ponena za Yehova Mulungu Wathu pamene anachita utsutsi kwa anthu ena ndipo motero, anatchedwanso *“Satana”*. Tikhoza kudziwanso kuti liwu limeneri silimayimira uchimo wina uliwonse ayi. Choncho, liwu loti *“Satana”* likugwirizanadi ndi *“Tchimo”* m’njira yokhayo yakuti pa chibadidwe, munthu anabadwa mu uthunthu wa uchimo wa makolo ake, wotsutsana ndi Mulungu. Choteronso, ngati uthunthu umenewo ukhazikika mwaife, ndichimene chingatchulidwe *“Satana”* popeza chikutsutsana ndi umoyo wachilungamo umene Mulungu amawufuna. Komanso kagwiritsidwe ntchito ka mau amenewa kakuonetsa kuti khalidwe lotsutsa kapena malankhulidwe otsutsa ndi amene amatchedwa *“Satana”* M’Baibulo. Uwu ndiwo mtsutso wa chilungamo kapena tinenenso kuti mtsutso wa choonadi ndi chiyero. Mulungu Iye Mwini angakhalenso kapena akhoza kuchulidwanso *“Satana”* kwaife pamene tipereka mayesero kwa anzathu; komanso ngati atitsutsa pa zimene tifuna kuzichita. Mwinanso ngati tilankhula zotsutsana ndi Mulungu kapena aliyense amene akuchita kufuna kwa Mulunguyo, Mulungu akhoza kukhala Satana kwa ife. Mwaichi, sitinganene kuti Mulungu ndi wochimwa popeza watchulidwa kuti ndi *“Satana”* kapena kuti popeza watitsutsa ife pa zoyipa zimene timachita ayi. Chimene tiyenera kudziwa apa ndi chakuti pali Satana wabwino ndinso woyipa. Kotero, anthu ambiri sakumvetsa tanthawuzo la liwu loti *“Satana”*. Tiyeni choncho, tidziwe zeni zeni kutidi tchimo limatchulidwa kuti ndi satana chifukwa zochitikazo mtchimolo zimatsutsana ndi zimene Mulungu amafuna kuti ife tizichita tsiku ndi tsiku.

M’mabuku a Samueli ndi Mbiri, muli nkhani zambiri zimene zidalembedwa motsagana komanso mofanana. Tiona kuti nkhani zomwe zinalembedwa m’Buku la Mbiri ndi zimenenso zinalembedwa m’Buku la Samueli zikufanana kapena tinene kuti ndi nkhani imodzi imene inabwerezedwa kulembedwa; monganso timaona kuti m’mabuku a Uthenga Wabwino, mau omwe analembedwa ndi alembi aja anali amodzi modzi omwewo ngakhale kuti

kalembedwe ka nkhanizo ndi kosiyaniranapo pang'ono poyerekeza ndi m'mene tingawerengere nkhani yomweyi m'Buku lina lotsagana nalo m'Chipangano chomwecho yalembedwera. Tipereke chitsanzo: 2 Samueli 24:1 analembe kuti ***“Ndipo mkwiyo wa Yehova unayakanso pa Israeli, nafulumiza Davide pa iwo”*** kotero, kuti Davide uja achite changu, achite kalemba wa ana a Israeli. Timawerenganso nkhani yomweyi pa 1 Mbiri 21:1 pomwe timamva kuti ***“Pamenepo, Satana anaukira Israeli, nasonkhezera Davide awerenge Israel!”*** Tikapitiriza kuwerenga nkhani imeneyi, tipeza kuti nkhaniyi m'mabuku awiri amenewa ndi imodzi yomweyo yonena za kuwerenga ana a Israeli pofuna kukwaniritsa chinthu chimodzi chimene Mulungu anafuna kuti chichitike. M'Buku lina tamva kuti Mulungu ndi amene anadzutsa Davide, pamene m'Buku linalo Satana ndi amene anadzutsa Davide uja. Tiona kuti Davide anadzutsidwa ndi cholinga chimodzi kuti cholinga cha Mulunga chimodzi chija chikwaniritsidwe, Davide ndiye anayenera kukwaniritsa kapena kumvera lamulo la Mulungu panthawiyo. Mwaichi, ndizodziwikiratu kuti Satana amene akukambidwa m'Buku la Mbiri uja anali Mulungu yemwe akukambidwanso m'Buku la Samueli. Yehova anatchulidwa ***“Satana”*** m'Buku la Mbiri chifukwa chakuti adasiyana maganizo kapena tinene kuti anatsutsana ndi zimene ana a Israeli anakonda kuchita. Kotero, Mulungu analidi Satana kwa Davide ndi ana onse a Israeli. Mulungu anakhalanso Satana kwa Yobu pamene analola kuti Yobu abvutike ndi milili ya matenda yosiyana siyana kotero, Yobu ananena, ***“Ndidzanja lanu mudzitsutsa pondizunza ine”*** (Yobu 30:21). Pano, tiona kuti Yobu akunena mwanjira ina kuti ***“Inu Ambuye mwakhala Satana wanga”*** m'ndime imeneyi.

LIWU LONENA KUTI ‘M’DIEREKEZI’ M’BAIBULO

Monga taona tanthawuzo la Satana, liwu loti Mdierekezi nalonso siliyimira chinthu china chiri chonse chamoyo ndi champhamvu padziko lapansi. Yesu anati, ***“Kodi sindinasankha inu anthu khumi ndi awiri (akuphunzira ake) ndipo m'modzi wainu ndi mdierekezi? Iye anakamba za Yudase Isikariote...”*** amene adali munthu wamba, wokhala ndi moyo wakufa. Iye sanalankhule kwa chinthu china chonyansa chosafa, champhamvu zochimwitsa anthu ayi, koma kwa Yudase. Pano liwuli likamba ndinso kutanthawuza za munthu amene ali ochimwa osati za chinthu chimene chinachimwitsa Yudase ayi. Chitsanzo china tingachipeze pa 1 Timoteo 3:11. Akazi a akulu a mpingo analangizidwa kuti sadayenera kukhala ***“olemekeza”*** osati ***“odierekeza”***; apa liwu la m'chi Greek ndi ***“diabolosi”*** lomwe ndi liwu

limene linamasuliridwa kuti *“Satana”* ndinso *“devil”* m'malo ena a m'Baibulo. Choncho, Paulo akuchenjeza Tito kuti amayi okalamba mu Eklesia wa Mulungu asakhale *“adierekezi”* kapena *“devils”* i.e *“achinyengo” etc* (Tito 2:3). Moteronso, Paulo anawuza Timoteo (2 Timoteo 3:1,3) kuti *“m'masiku otsiriza ...anthu adzakhala...odierekeza”*. Izi sizitanthawuza kuti anthu amenewa adzasandulika nakhala zinthu zoopsa zamphamvu, zimene ziri ndi nyanga monga ena amanenera ayi; koma kuti anthu amenewa adzasokera, ndi kuchita zosabvomerezeka pamaso pa Mulungu chifukwa chakudziyerekeza kwao. Ndizomveka bwino lomwe kuti liwu loti *“mdierekezi”* kapena *“Satana”* sakuyimira m'ngelo wina aliyense amene adagwa panso pano kuchokera kumwamba monga ena amaganizira ayi, kapenanso kuti ndi chinthu china chake chapadera choopsa chimene chimabweretsa uchimo mwaife ayi koma anthu *odzierekeza*.

MATANTHAUZO A MAU OTI: ‘TCHIMO’, ‘SATANA’ NDI ‘MDIEREKEZI’

Mau onena kuti “Satana” ndi “Mdierekezi” amagwiritsidwa ntchito m'chiphiphiritso ponena za zokonda, chikhalidwe ndi chilakolako cha uchimo mwaife anthu, zimene takambanso m'Phunziro 6.1. Zimenezi ndizo a “Satana” ndi a “Dierekezi” athu otsutsana ndi zolinga za Mulungu lero lino. Mau amenewa amakambidwa ngati anthu kotero, timawerenga za mau'wa ngati zinthu zeni zeni za moyo makamaka ngatidi anthu eni eni; Mwaichi, “Mdierekezi” – mdani wathu, ndiye owononga choonadi. Motero, ife maganizo athu a umunthu mwaifeyo ndiwo “Mdierekezi” waife tokha. Kugwirizana pakati pa umunthu wathu ndi zilakolako zathu ndizo “tchimo la mkati mwa mitima yathu” ndipo Mau Oyera akuti; *“...Popeza tsono ana* (ndife ana muuzimu) *ndiwo ogawana m'mwazi ndi thupi, Iyenso* (Yesu) *momwemo adalawa nawo makhaliidwe omwewo kuti mwa imfa* (yake) *akamuononge iye amene anali nayo mphamvu yaimfa, ndiye mdierekezi:”* (A Hebri : 2:14). Mdierekezi pano, tamva kuti ndiye gwero la imfa. Kutanthauza kuti ndiye amabweretsa imfa. Koma timawerenga kuti *“mphototho yake ya tchimo ndiyo imfa”* (Aroma 6:23). Choncho, apa ndiye kuti zikutanthauzanso kuti uchimo ndi “Mdierekezi” ndi chinthu chimodzi chomwecho. Chifukwa chake tamva kale kuti ndizo gwelo kapena tinene kuti chiyambi cha imfa. Zonsezi chotsatira chake ndi imfa motero, udierekezi ndiwo uchimo! Mofanana ndi ndime yomweyi, Yakobo 1:14 akunenetsa kuti ndithudi, zilako lako zathu ndizo zimatitengera ife ku chiyeso chimene

chotsatira chake ndi utchimo. Tawerenganso pa A Hebri 2:14 kuti Mdierekezi amabweretsa imfa. Koma tawerenganso m'ndime yomweyi kuti Yesu adabadwa m'maonekedwe ndi mthupi longi lathuli n'cholinga chakuti aphwasule ndi kuthana ndi mdierekezi. Tsopano siyanitsani nokha izi ndi Aroma 8:3:- **“...Mulungu anatomiza Mwana Wake wa Iye Yekha m'chifanizo cha thupi la uchimo** (kutanthauza kuti mthupi ngati lathu lino), **natsutsa uchimo mthupi**). Izi zikuonetseratu kuti khalidwe la kudziyerekeza ndiwo uchimo ndipo kuti izi zimachitika mu uthunthu wa thupi lathu lino koteronso zonse ndi zochitika ndi chinthu chimodzi chomwecho. Nkofunikiranso kumvetsa kuti Yesu anayesedwa m'thupi monga ifenso timayesedwa m'thupi, mzilako lako za thupi lathu zimene zimatsutsana ndi chifuniro cha Mulungu. Ngati wina sangamvetse bwino ndondomeko imeneyi, yomwe idakhazikitsidwa ndi Mulungu pachiyambipo, ndiye kuti nkobvuta kwaiye kukhutitsidwa komanso kuzindikira chindunji cha umunthu wathu ndinso umunthu wa Yesu Khristu koteronso, sadzatha kudziwa ndi kumvetsa bwino za ntchito ya Yesuyo. Popeza Yesu Khristu adaali ndi thupi ngati lathuli, Iye adaalinsu ndi udierekezi m'thupi lake monga ife timakhala ndi udierekezi m'matupi athu (zilakolako za chibadidwe zoyerekeza) kotero, ichi chingatilimbikitse koposa kukhala ndi chiyembekezo cheni cheni cha chipulumutso (A Hebri 2:14-18; 4:15). Posafokera mzilako lako zathupi lake zomwensu zikuyimira udierekezi wa m'Baibulo, Yesu anaphwasula m'dierekeziyu pa mtanda paja (A Hebri 2:14). Ngati m'dierekezi ndi chinthu china chamoyo komanso champhamvu monga ena amanenera, ndiye kuti panopa bwezi m'dierekeziyo kulibe popeza tikumva kuti anaphedwa (anaphwasulidwa) ndi Khristu pamtanda. A Hebri 9:26 akunena kuti Yesu anaonekera mu umunthu **“...kuchotsa uchimo mwa nsembe ya Iye yekha”**. A Hebri 2:14 akugwirizana ndi mfundo imeneyi ponena izi kudzera mu imfa yake kuti, Khristu anapha ndi kuthetsa m'dierekezi amene anali mwa Iye yekha. Mwaimfa yake, Yesu anathetsa **“thupi la uchimo”** (Aroma 6:6), mwachitsanzo, thupi la umunthu, uchimo umene unawululidwa mu zilako lako za thupi lathu lino, komanso zoyipa zimene zimawonekera m'matupi athu ofooka.

“Iye wochita tchimo ali wochokera mwa m'dierekezi” (1 Yohane 3:8), chifukwa tchimo ndicho chotsatira chakufooka kwathu, ndikugonjera zilako lako za matupi athu (Yakobo 1:14,15), zimene m'Baibulo zimatchulidwa mchiphiphiritso kuti **“m'dierekezi”**. **“Chifukwa chaichi, Mwana wa**

Mulungu adaonekera kuti akaononge m'dierekezi” (1 Yohane 3:8). Ngati tikunena zoonadi kuti m'dierekezi ndi zilako lako za m'mtima mwathu zomwe ndi ntchito zoyipa mwaife, ndiye kuti ntchito zimenezi ndizo machimo athu. Mfundo yotereyi ikutsimikizidwanso pa 1 Yohane 3:5: *“Iyeyu (Yesu) anaonekera kudzachotsa machimo athu”*. Apa ndime imeneyi ikuonetsanso motsimikiza kuti *“machimo athu”* ndinso *“ntchito za mdierekezi”* ndi chinthu chimodzi chomwecho. Machitidwe 5:3 akupereka chitsanzo china choonetsa kugwirizana pakati pa mdierekezi ndi machimo athu. Petro akunenetsa kwa Ananiya kuti: *Satana anadzaza mtima wako chifukwa ninji?*” Kenaka Petro m'ndime ya chinayi akuti *“bwanji chinalowa ichi mu mtima mwako? Sunanyengatu anthu koma Mulungu”*. Kusunga chinthu choyipa mumtima mwathu, ndi chimodzimodzi kunena kuti *“Satana wadzaza mumtima mwathu”*. Ngati ife patokha tidzisungira chinthu, mwachitsanzo, maganizo ochita choyipa, zonsezi zimayambira mkati mwa mitima yathu. Tikamva kuti mkazi wayima, chimakhala chinthu chochitika mkati mwathupi lake osati kunja kwathupi lake ayi. Yakobo 1:14,15 akufotokozera bwino nkhani imeneyi ya gwero la tchimo pofuna kupereka chithunzi-thunzi choyenera cha chiyambi cha tchimo mwaife kuti ndicho *zilako lako za m'mitima mwathu komanso mogwirizana ndi chitsanzo cha kuyima kwa mzimayi poyembekezera kubadwa kwa mwana*; Mayi akayima, chotsatira chake amabala mwana ndipo momwemonso, zilako lako za m'mitima mwathu zimabala uchimo – chomwe chotsatira chake ndiyo imfa. Buku la Masalmo 109:6 likunenaponso nkhani yomweyi mofananiza munthu wochimwa ndi “Satana”; *“Muyike munthu woyipa akhale mkulu wake; Ndi mdani (Satana) ayime padzanja lamanja lake;”* Chitsanzo, mwamphamvu zopitirira Iye (Masalmo 110:1).

KUKAMBA ZA CHINTHU POYEREKEZA NGATI KUTI NDIRIMUNTHU

Mwina nthawi zina mukhoza kunena kuti “Koma apa mdierekezi akukambidwa ngati kuti ndi munthu!” Izi ndi zoonadi; A Hebr 2:14 akunena za *“Iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye Mdierekezi;”*. Ndipo ngakhale kuwerenga pang'ono Baibulo nthawi zambiri tiona kuti limakambabe za zinthu zambiri ngati kuti ndi anthu mwachitsanzo, kukamba za zinthu zosaoneka ndi maso ngati kuti ndi anthu. Moteronso, Miyambo 9:1 akufotokoza za liwu la chizimayi limene likutchedwa **“nzeru”** kuti imanga nyumba, ndipo Aroma 6:23 akuyerekeza tchimo ngati kuti ndi munthu amene

alipira malipiro omwe ndi (chotsatira chake ndicho) imfa. Mbali imeneyi ya Mdierekezi yafotokozedwa kale mwatsatane tsatane pa ndime ya Mpatuko 5. Mdierekezi amene tikukambirana panoyi, yemwense ena amati “diabolosi” ndi amene akuyimira zilako lako zonse zoyipa mu mitima yathu. Ngakhale ziri choncho, tonse tikudziwa kuti palibe m’modzi waife angafotokozere motsimikiza kuti “diabolosi” kapena “mdierekezi” anamuonapo. Tikudziwanso kuti zilako lako m’mitima yathu sizingaoneke ndi maso athu ayi koma tikhoza kuona zotsatira zake komanso kuti zonsezi sizingayende pazokha popanda munthu. Choncho, tadziwa tsopano kuti liwu limeneri la mdierekezi likungotanthauza zilako lako zathu mwaiife zimenenso zimakambidwa ngati kuti ndi munthu; poonanso kuti mdierekezi ndi liwu lina loyimira uchimo mwaiife anthu. Tchimo limakambidwa ngati *bwana* pa Aroma 5:21; 6:6,17; 7:3. Ndizomveka choncho, kuti mdierekezi sichinthu, simunthu, sichinyama kapena chilombo, simngelo monga ena amanenera ayi, koma kuti ndi chiphiphiritso kapena tinene kuti dzina lina lozembera pofotokoza za tchimo. Mnjira yomweyi, Paulo akunena zaife kuti tiri ndi maganizo awiri monga zinaliri nthawiyo; mwathupi lathu lino (Aroma 7:15-21): Munthu wa thupi, **“Mdierekezi”** amene amalimbana ndi munthu wa (*maganizo a*) uzimu. Komabe apa sizitanthauza kuti anthu awiri amene takamba apawa ndi anthu eni eni ayi, koma kuti ndiwo maganizo awiri osiyana chabe m’mitima yathu. Maganizo athu oyipawo ndi amene akutchedwa **“Mdierekezi”**. M’Baibulo mdierekezi, liwu limene m’chi Greek limatanthawuzanso kuti **“Oyipayo”** pano likumasuliridwa kuti **“munthu wochita zoyipa”** pa 1 Akorinto 5:13, kuonetsa ndithu kuti pamene munthu agonjera ku tchimo, makhaliidwe ake “ochita zoyipa” – amenenso ali maganizo a **“iye mwini”**- payekha, amakhala “munthu wochita zoyipa” – **Mdierekezi**.

“MDIEREKEZI”, “SATANA” KUONEKERA MZINTHU ZOCHITA ANTHU A NDALE NDI A BOMA PADZIKO

Mau oti *‘mdierekezi’* ndi *‘satana’* amagwiritsidwa ntchito pofuna kufotokozera za anthu oyipa komanso ochimwa amene akhala mdziko lino lapansi limene ife lero lino tikukhalamo. Chikhalidwe chathu, ndale zathu ndinso umoyo wathu wa chikhristu chosayenera zonse zimathanso kukambidwa ngati *‘mdierekezi’*. Mdierekezi kapenanso satana m’Chipangano Chatsopano nthawi zambiri zinkakambidwa pofuna kunena za ulamuliro wa a Yuda ndi Aroma. Nchifukwa chake timamva kuti okhulupirira ambiri adaponyedwa m’ndende ndi mdierekezi (Chibvumbulutso 2:10), ponena momwe akulu akulu a boma la

Aroma ankamanga okhulupirira a nthawi imeneyo. M'njira yomweyi, timawerenganso kuti tcharitchi ya Pergamo inali kufupi ndi mpando wa satana. Ulamuliro wa boma la chi Roma unkafuluza koposa zinthu zonse zimene okhulupirira a Yesu Ambuye Wathu ankachita. Apa sizikutanthauza kuti satana (chinthu cha mtundu wina wake oopysa) ndi chimene chinali ndi mpando wachifumu ku Pergamo, ayi. Uku kunali kufotokozerana zinthu zomwe zinkachitika m'nthawi ya m'aulamuliro a maboma amene ankatsutsana ndi umoyo wa chikhulupiriro choonadi cha anthu ena omwe ankakhala mu mzinda wa Pergamo.

Tchimo limanenedwa ngati kulakwila lamulo la Mulungu (1 Yohane 3:4). Koma tchimo limene limafotokozedwa kuti ndilo chikhalidwe ndi maulamuliro otsutsana ndi Mulungu, ndiyo mphamvu yoposa mwa anthu; mphamvu imene imapereka mazunzo kwa anthu wamba, ana a Mulungu, omwe ndi osauka; komanso onse ofedwa ndi amene amazunzika ndi mphamvu yonyansa imeneyi. Maudindo onse amene apanga lamuliro lomwe komalizira kwake limakazunza anthu, ndi amene nthawi zina amakambidwa ngati chinthu chamoyo chokhala ngati munthu kapena chilombo choopysa chimenenso chikutchedwa 'mdierekezi' m'Baibulo. Motero, mayiko a Irani ndi ena a chisilamu anatchulapo dziko la United States kuti ndilo "satana wamkulu" mwachitsanzo, chifukwa chakuti ndi dziko limene limatsutsa kwambiri zochita za mayiko amenewa pa ndale, kapenanso pa chipembedzo chawo. Umu ndi m'mene mau oti "mdierekezi" ndi oti "satana" amagwiritsidwira ntchito m'Baibulo pofotokozerana mbali zosiyana siyana.

Pomaliza, tiyenera timvetse ndipo tizindikire kuti Baibulo ndilo Mau okhawo obvomerezeka ndi Mulungu, ndipo kuti ife tizitsata malamulo akewo opezeka m'Baibulo. M'malo momangotsamira pa timanunsu tochepe chabe, tiyeni tiwerenge mozama ndi modzipereka nkhani zonse zokhudza mutu umene tikuwerengawo kuti timvetse bwino mfundo imene tayiyambayo ndipo tikatero, tidzazindikira koposa. Phunziro limeneri la 'mdierekezi' ndilo limodzi lofunikira kulimvetsa bwino pa chikhulupiriro ndi chipulumutso chathu. Ife tingapindule kwambiri ngati tingawerenge popemphera, kutsindika ndi kudzipereka kotero tikadziwe zoonza zeni zeni zimene zimapezeka m'Baibulo. Tiyeni tizindikire zonse zimene zalembedwa m'Phunziro 6.1 motsindika makamaka gawo lonse la Phunziro 6.1 pomwense palembedwa za 'mdierekezi' ndi 'satana'. Tikawerenga modzipereka ndi mozindikira chimene tikuchita pa nkhani zimenezi, tidzaona Mau a Mulungu m'ndime zina ndi zina,

kuti amathadi kupereka mfundi imodzi, mogwirizana komanso kuti amatha kugwiritsa ntchito mau amenewa (mdierekezi, satana) ngati mau ofotokozera zambiri za ntchito, zochita za anthu ndi zinthu zina. Ndipo n'chifukwa chake kawiri kawiri mau amenewa amalembedwa pofuna kunena zambiri zokhudza machimo pakati pathu ife anthu. Ndime zambiri zimene ena samazimvetsa bwino, zafotokozedwa mwatsatane-tsatane m'mipatuko imene yalembedwa komaliza kwa Phunziro lino.

Anthu ena onse omwe sakukhutirabe ndi zimene mwawerenga m'Phunziro limeneri ayenera adzifunse kuti: Kodi tchimo linalembedwapo ngati munthu m'Baibulo pamene Adamu anachimwa? Tikawerenga Baibulo mofatsa, tiona kuti izi ndi zoono. Kodi ndi zoono kuti liwu loti *Satana* lingagwiritsidwe ntchito ngati liwu lofotokozera kapena lokamba zambiri zokhudza ntchito ya munthu? Izinsu tikudziwa kuti ndi zoonanso. Choncho, chikutibvuta tsopano ndicho kubvomereza mfundo zolembedwa m'Baibulo zimenedi zikutifotokozera zambiri zokhudza mau a '*mdierekezi*', '*satana*' ndi '*tchimo*' ngati anthu kapena kuti ngati zinthu zamoyo zoopysa. Dziko lonse nthawi zambiri limakambidwanso ngati anthu mkalata ya Yohane ndi m'mabuku a 'Uthenga Wabwino'.

6.3 DAIMONI (MIZIMU YONYANSA)

Mitu iwiri takamba m'mwambayi takambirana zinthu zingapo ndipo taona zifukwa zosiyana siyana zimene sizikuonetsa kuti *mdierekezi* kapena kuti *satana* ndi zinthu zamoyo zowoneka ngati zirombo kapena anthu ndi maso athu. Ngati zimene takambirana zingakhale zoono, ndiye kutinsu zikhulupiro za mizimu yoipa (demoni) zimene anthu amati ndi antchito a mdierekezi, kulibe sizingapezeke pena paliponse. Ambiri amaganiza kuti Mulungu amatipatsa ife anthu zinthu zabwino zokha zokha, ndipo kuti mdierekezi yemwe ndi mizimu yake yoipa ya satana imatipatsa ife zinthu zoipa zokha zokhanso. Ndipo amapitirizanso kuti mdierekezi amatilanda zinthu zabwino zomwe Mulungu amatipatsa zija kuti tisakhale nazo koma tizizunzika.

Tibwereze pano kunena kuti Baibulo lomwe ndi Mau ake a Mulungu , limatiphunzitsa momveka bwino, mosadzitsutsa komanso mosaphonya kuti Yehova ndiye amene ali gwelo lalikulu la Mphamvu zonse padziko lapansi (onaninso Phunziro 6.1), ndipo kuti ndiyenso amabweretsa zinthu zabwino ndinso zoyipa m'miyoyo yathu:-

“Ine ndilenga kuyera ndi mdima, Ine ndilenga mtendere ndi choyipa, Ine ndine Yehova wochita zinthu zonse zimenezi” (Yesaya 45:7).

“Pakuti wokhala m'Maroti alindira chokoma, popeza choyipa chatsika (kuchokera) kwa Yehova kumka ku chipata cha Yerusalemu” (Mika 1:12).

“Kodi adzaomba lipenga m'mudzi osanjenjemera anthu? Kodi choyipa chidzagwera mudzi osachichita Yehova?” (Amosi 3:6).

Mwanjira imeneyi tikapeza mayesero, tiyenera kubvomereza kuti mabvuto amenewa akuchokera kwa Mulungu, posamuda satana, mizimu yoipa kapena mdierekezi kuti ndiamene watipatsa mabvutowo. Yobu anataya zinthu zake zabwino zambiri zimene zimachokera m'madalitso a Yehova koma sananenepo kuti ***“mizimu yoipa iyi yandilanda zinthu zonse zimene Mulungu anandipatsa”*** ayi; imvani zomwe iye ananena:-

Yehova anapatsa, Yehova watenga, lidalitsike dzina la Yehova” (Yobu 1:21).

“Ha! Tidzalandira zokoma kwa Mulungu kodi, osalandiranso zoyipa?” (Yobu 2:10).

Tikamvetsa mfundo zimenezi kuti zinthu zonse zabwino kaya zoyipa zichokera kwa Mulungu, tidzakhala anthu a chiyembekezo choyenera ndinso champhamvu kotero, tikakhala ndi mabvuto, tidzayesetsa kupempha molimbika kwa Mulunguyo kuti atichotsere zoyipazo pakati pathu, komanso kuti ngati zoyipazo sizikutichoka, ndiye kuti zikutibwerera ncholinga chakuti tiphunzitsidwe kanthu kena kamene mwina ife sitinachite bwino. Koteronso, komalizira kwake ife tidzapindula tikazindikira choyipa chathu. ***“Mwana wanga usayese chopepuka kulanga kwa Ambuye, kapena usakomoke podzudzulidwa ndi Iye (osati kudzudzulidwa ndi mizimu yoipa!)”***; ***pakuti iye amene Ambuye ankonda amlanga, namulanga, namkwapula mwana aliyense amlandira. Mukapirira kufikira kulangidwa Mulungu achitira inu monga ngati ana; pakuti mwana wanji amene atate wake wasamlanga? Koma ngati mukhala wopanda chilango, chimene onse adalawako, pamenepo muli a m'thengo, siana ayi”*** (A Hebri 12:5-8).

MULUNGU: GWELO LA MPHAMVU ZONSE

Mulungu ndiye gwelo ndi mwini wake wamphamvu zonse:

“Ine ndiri Yehova, ndipo palibe winanso; popanda Ine palibe Mulungu wina (liwu limene lamasuliridwa kuti Mulungu pano limatanthauza kuti ‘mphamvu’ m’chi Hebri) ; ndidzakumanga m’chiuno ngakhale sunandidziwa;” (Yesaya 45:5);

“Kodi popanda Ine aliponso Mulungu? ‘Iai, palibe thanthwe; sindidziwa lirilonse’; atero Yehova”. (Yesaya 44:8);

“Yehova ndiye Mulungu; palibe wina opanda Iye”. (Deuteronomo 4:35).

Ndime ngati zimenezi ziripo zambiri m’Baibulo zimenedi zikutitsimikizira ndithu kuti Mphamvu ndi zonse zochitika padziko kwaife lero lino, zimachokera kwa Yehova mwini. Chifukwa chakuti Mulungu ndiye mwini Mphamvu ndipo kuti palibenso wina, Chiuta ali Mulungu wansanje monga amatikumbutsa nthawi ndi nthawi kosatha (Eksodo 20:5; Deuteronomo 4:24).

Mulungu amakhala wansanje pamene anthu ake ayamba kupembedza milungu ina mwachitsanzo, ngati anena kuti: *“Inu ndinu Mulungu wamphamvu, wamkulukulu, komabe ife tidziwanso milungu ina pamwamba painu, ngakhale kuti milungu imeneyi siiri ya mphamvu koma tiyidziwabe”.* Ichi ndi chifukwa chake sitiyenera kukhulupirira za mizimu ndi mdierekezi kuti ziri ndi mphamvu pamenenso tikudziwa ndi kubvomereza kuti kuli Yehova m’modzi yekhayo; Tiyeni tibvomereze motsimikiza kuti Mulungu Yehova m’modzi’yo ndiye woono. Motero, tikalolera kuti mdierekezi ali ndi mphamvu yapadera, likhala tchimo kwaife, limenenso ana a Israeli adachita kotero analakwiladi Chiuta wao. Chipangano Chakale kwambiri chimaonetsa mmene ana a Israeli anamukwiyitsira Mulungu wao pokhulupirira milungu ina pamwamba pa Chiuta woonadi. Tiona tikawerenga m’Baibulo kuti mizimu (daimoni) imene anthu amayikhulupirira kawiri kawiri lero, ndiyo milungu imene ana a Israeli ankayikhulupiriranso nthawi imeneyo.

MIZIMU (DAIMONI) MILUNGU (ZIWANDA)

M’buku la 1 Akorinto, Paulo akufotokozerana chifukwa chimene akhristu sankayenera kupembedza mafano kapena kukhulupirira m’chipembedzo cha mafano ayi. M’nthawiyo anzathu amene ankawerenga Baibulo mozama, anthu ena ankakhulupiriranso kuti mizimu inali milungu yao yaing’ono-ing’ono imene inkapembedzedwa ncholinga chothetsa mabvuto awo omwe ankakumana

nayo m'miyoyo yawo. Chifukwa cha chikhulupiriro chimenechi, iwo ankasema ziboli boli zomwe ankazona ngati mizimu kapenanso kuti milungu yao yomwenso ankayigwadira nkumayipembedza. Apa tidzaona kuti kunali koyenera kuti Paulo agwiritse ntchito mau amenewa (*mizimu ndi milungu komanso mafano*) mofanana mkalata yake iyi:-

“Koma nditi kuti zimene amitundu apereka nsembe azipereka kwa ziwanda osati kwa Mulungu; ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda... Koma ngati wina akati kwa inu, Yoperekedwa nsembe iyi kwa mafano, musadye m'malo mwaiye” (1 Akorinto 10:20,28).

Choncho, mafano ndi ziwanda zikuonekeratu kuti mau'wa ndi ofanana m'matanthauzo ake. Onaninsu m'mene Paulo akunenera za nsembe imene inkaperekedwa ***“kwa ziwanda*** (mafano) osati ***kwa Mulungu”***. Ziwandazo pano tingati sizidaali Mulungu ndipo popeza kuti pali Mulungu m'modzi, nkoyenera kudziwa kuti milungu/ziwanda zilibe mphamvu ina iriyonse ayi, izo si milungu. Mfundo imeneyi ikutsimikizidwa tikawerenga 1 Akorinto 8:4:-

“Tsono kunena za kudya zoperekedwa nsembe kwa mafano, tidziwa kuti fano (lofanana ndichiwanda);siliri kanthu padziko lapansi, ndi kuti palibe Mulungu koma m'modzi”

Fano, kapenanso chiwanda chilibe moyo wamtundu wina uliwonse. Tidziwa kuti pali Mulungu m'modzi woonadi, wamphamvu zopanda malire mdziko lonse. Paulo akupitiriza nkhani imeneyi (m'ndime 5,6 zotsatirazi) motere:-

“Pakuti ngakhale pakhalenso milungu ina yotchedwa milungu (monga pali milungu yambiri, ndi ambuye ambiri, [komanso ngati m'mene anthu akhulupirira kuti kuli ziwanda lero lino, chiwanda china chothetsa ntchito ya munthu, chiwanda china chothetsa maukwati a anthu, ndi zina zotere]) Koma kwaife,(tonse okhulupirira) pali Mulungu m'modzi, Atate, amene anapanga zinthu zonse (zabwino ndi zoyipa, ngati m'mene tawerengera m'ndime zapatsidwa kalezo)”

Popitiriza kuona mfundo imeneyi m'Chipangano Chatsopano, ziwanda zinkaonekeratu kuti ndi mafano, kapena tinene kuti milungu ina (Daimoni) monga tingawerenge pa Machitidwe 17:16-18; umu ndi momwe Paulo analalikirira ku Atene kumene chipembedzo chimenechi cha mafano chinali chitakhazikika kale kwambiri; choncho, anthu akumeneko ankapembedzadi milungu yambiri. Anthu atamva ulaliki wa *uthenga wabwino* wa Paulo, anati ***“Ichi chiyani afuna kunena wobwetuka uyu? ‘Ena naati,’ Anga olalikira***

ziwanda zachilendo (mizimu kapena milungu yachilendo), *chifukwa analalikira Yesu ndi kuukanso kwa akufa*” Choncho apa, zikutanthauza kuti anthu amenewa anamva komanso anazindikira mwatchutchu kuti Paulo adalalikira za ‘Yesu’ ndi *“kuukanso kwa akufa”* ngati kuti ndi ziwanda, kapena tinene kuti mizimu, kayanso milungu yatsopano imene idaalidi ya chilendo kwa anthu a mu mzindawo. Mukapitirira kuwerenga nunsu imeneyi mutha kuona nokha m’mene Paulo anaongolera mfundoyi polalikira motsindika zachoonadi kwa anthu amenewa, ndipo pa ndime ya 22 iye akuti, *“Inu muli a zipembedzo za makolo”* (kutanthauza kuti ndithu, iwo anali opembedza mafano, ziwanda kapena tinenenso kuti mizimu); ndipo akufotokoza m’mene Mulungu amakhalira ndi kuti Yehova sangapezeke mwa ziwanda kapena mafano ayi.

Tiyenera kukumbukira kuti Mulungu ndiyekhayo amene ali ndi mphamvu. Ngati Iye sangapezeke mwa ziwanda, ndipo kuti sangakhale chiwanda, ndiye kuti ziwandazo kapena mafanowo zonse zilibe mphamvu zoposa za Mulungu popeza tidziwadi palibenso gwelo lina lirilonse padziko lapansi kaya pansi pa thambo la kumwamba, kaya kungsi kwa nthaka, lokhala ndi mphamvu kuposa Mulungu Yehova. Mwaichi, zonsezi sizamoyo ayi koma zakufa.

ZIWANDA M’CHIPANGANO CHAKALE ZIDALI MAFANO

Tikabwerera pang’ono m’mbuyo m’Chipangano Chakale, pali chitsimikizo chokwanira kuti *“ziwanda”* ndi chimodzi-modzinso liwu loti *“mafano”*. Deuteronomo 28:22, 59-61 adaneneratu maulosi kuti matenda ambiri aubongo adzakhala njira imodzi yokhaulitsira ana a Israeli chifukwa ankapembedza mafano / ziwanda. Nchifukwa chake m’Chipangano Chatsopano, matenda onse okhudza ubongo wa munthu, amakambidwa ngati kuti ndi matenda a ziwanda. Koma tiyeneranso kuona kuti mau ambiri okhudza ziwanda kapena tinene kuti mizimu, amagwirizana ndi matenda okhudza ubongo wa munthu, osati tchimo malingana ndi m’maganzidwe a anthu. Sitanawerengepo kuti Yesu anachiza ziwanda zoyambitsa nsanje, umbanda ndi zina zotere ayi. Onaninso kuti Baibulo limakamba za anthu okhala ndi matenda/ziwanda osati kuti ziwandazo ndi zimene zimayambitsa matendawo ayi. Tikawerenga Baibulo la chi Greek (Septuagint) tiona kuti liwu loti *“daimoni”* limagwiritsidwa ntchito m’malo mwa liwu loti *“fano”* (Deuteronomo 32:17 ndi Masalmo 106:37; Iri ndilo liwu limene linamasuliridwa kuti *“ziwanda”* (demoni) m’Chipangano Chatsopano. Masalmo 106:36-39 tiwerenga kuti

Israeli analakwira Mulungu popembedza mafano ndipo akunenanso kuti mafano amenewa ndiwo ziwanda monga Israeli anakhulupirira m'mafano osiyana siyana:-

“Ndipo anatumikira (ana a Israeli) mafano awo, Amene kwa iwo unali msampha wakuwakola: Ndipo anapereka ana awo amuna ndi akazi (ngati) nsembe ya kwa ziwanda, Nakhetsa mwazi wosachimwa, ndiwo mwazi wa ana awo amuna ndi akazi, Amene anawapereka ngati nsembe kwa mafano a ku Kanani; M'mwemo analidetsa dziko ndi mwaziwo. Ndipo anadzũpsa nazo ntchito zawo, Nachita chigololo nao machitidwe awo.”

Apa tikhoza kuona kuti ziwanda sizikusiyana m'matanthauzo ndi liwu loti **“mafano”** kotero, chiwanda ndi dzina lina la **“fano”** monga taona powerenga ndime zimene zapatsidwa pamwambazi. Chipembedzo chawo cha ziwanda, Mulungu akuchitcha kuti kupembedza **“ntchito za manja awo”** chifukwa chakuti chikhulupiriro chawo chidatsamira pa mafano; zinthu zimene iwo anadzikonzera okha ndi manja awo komanso m'maganizidwe mwao. Choncho, onse amene amakhulupirira kuti ziwanda ndi milungu lero lino, akukhulupirira mzinthu zachabe, zopangidwa ndi manja a munthu, m'maganizo ndi chikonzero cha munthu osati zimene Mulungu watiphunzitsa ayi.

Deuteronomo 32:15-24 akunenanso kuti Mulungu Yehova amakwiya koopsa pamene anthu ake, olengedwa ndi Iye, akhulupirira mwa ziwanda: Israeli **“anasiya Mulungu amene anamlenga napeputsa thanthwe la chipulumutso chake. Anamchititsa (Yehova) nsanje ndi milungu yachilendo, Anautsa mkwiyo wake ndi zonyansa. Aziphera nsembe ziwanda, si ndizo mulungu ayi; milungu imene iwo sankayidziwa, imene makolo anu sanaiopa.....Ndipo Iye (Yehova) anati wopulukira, Ana osakhulupirira iwo Anautsa mkwiyo wanga ndi chinthu chimene sichiri mulungu; ...Ndizawaunjikira zoyipa paiwo.”**

Motero, taona kuti Mulungu sakusiyanita tanthauzo pakati pa mafano ndi ziwanda. Komanso tione kuti zoyipa zonse sizinthu zimene munthu ayenera kuzigwadira chifukwa zonsezi ziri chabe. Amene amakhulupirira ziwanda, amaonetseratu kuti alibe chikhulupiriro cheni cheni kwa Mulungu. Tikudziwa kuti sizingatheke lero lino kuti munthu akhoza kukhulupirira Mulungu Namalengayo kuti ndi amene amatipatsadi zonse pa moyo wathu, koma tidziwitsitse ichi; **“zabwino ndi zoyipa zonse zimachokera kwa Iye” (Yesaya**

45:5-7). Tikudziwanso kuti kwa munthu, nkosabvuta kukhulupirira kuti zinthu zonse zoyipa zimabwera kuchokera kwa chinthu china chake osati Chiuta ayi; Koma ife tikangokhulupirira kuti zonse zabwino ndi zoyipa zimachokera kwa Mphambe Namalenga wathu, ndiye kuti sikungakhale kobvuta kukhulupirira kuti wobweretsa zimenezi akhoza kuzichotsa mosabvutikanso, kotero, tidziwedi kuti Iye amene amabweretsa zimenezi ndiye Mulungu ndipo kuti nkosabvuta Iye Mwini kutichotsera zoyipazo nasiya zabwino zonse. Tidziwensho kuti mwina zoyipazo zatifikira n'cholinga chofuna kutiphunzitsa kanthu komanso kuti Mulungu afuna akwaniritse cholinga chake mwaife. Zonse ndi zopindulitsa kwaife tikapirira ngati ana ake eni eni a Mulungu.

CHIPANGANO CHATSOPANO CHIMANENANJI PA MUTU WA ZIWANDA

Ena a inu munganene kuti *'Bwanji ndime zochuluka m'Chipangano Chatsopano zikukamba za ziwanda?'* Chinthu chimodzi chimene ife tiyenera kumvetsetsa komanso kukumbukira ndicho kuti: Baibulo silingadzitsutse lokha chifukwa ndilo *Mau a Mulungu*. Ngati takhutira kuti Baibulo ndiwo Mau a Mulungu ndipo tamvetsetsa ndi kuzindikira kuti zoyipa ndi zabwino zonse zimadza ndi Yehova, ndipo koteronso Yehovayo ali mwini wa mphamvu zonse, ndiye kuti Baibulo silingatinamizedi komanso silingadzitsutse popeza Mulungu saali wachisokonezo ayi koma wa chilongosoko chabwino. Kotero tidziwadi kuti chikhulupiriro cha ziwanda ndi mafano chimatsutsana ndi chikhulupiriro cha mphamvu ya Mulungu Yehova. Iyi ndi mphamvu yomwe ingabweretse zabwino ndi zoyipa komanso kuchotsa zonsezi pa nthawi yoyenera. Zili ngati kuti Chiuta sangathe kuletsa ziwandazo kubweretsa zoyipazi kwa ife anthu ake ngati ziwandazo sizingabwere ndi Yehovayo. Tikafika apa, zikuonekeratu kuti liwu loti *'ziwanda'* linalembedwa kanayi kokha m'Chipangano Chakale ndipo kuti limapereka tanthauzo lofanana ndi liwu loti *'mafano'*. Koma tikaona m'Chipangano Chatsopano, liwuli lidalembedwa kambiri mbiri m'mabuku a *'Uthenga Wabwino'*. Ichi n'chifukwa chakuti, ziwanda (mafano) zinali ndikuti zili chabe ngakhale anthu ambiri adayamba kukhulupirira kuti kudziko kuno kuli zinthu zina zotchedwa ziwanda namazipembedza. Ziwanda monga tidziwira Baibulo kotero, sizingathe kuchiza kapena kugwira munthu nadwala monga anthu ena amakhulupirira ayi. Mulungu yekha ndi amene angachize matenda kapena kutichotsera choyipa china chiri chonse padziko lapansi. Kotero, n'chifukwa

chake munthu amene adalibe chitetezo cha Mulungu (chikhulupiriro mwa Yehova wa moyoyo) ankadwala matenda osiyana siyana m’Baibulo.

ZIWANDA (MILUNGU) M’CHIPANGANO CHATSOPANO

Pongonena kuti ziwanda zathamangitsidwa mwa munthu, zikutanthauzanso kuti munthu uja wachiritsidwa kumatenda okhudza ubongo, kapenanso kumatenda amene nthawi imeneyo sankadziwika bwino ndipo ankasowetsa mtendere pakati pa anthu. Anthu amene ankakhala m’chirumika choyambirira, ankaganiza kuti matenda alionse amene iwo sankawadziwa akawabwerera, ndiye kuti ankabwera ndi *‘ziwanda’* zomwe kwa iwo, zidaali zimene ankangoziganizira chabe kuti ndi zinthu zina zake zamoyo, zomwe zinkabweretsa mabvuto ndi matenda osiyana siyana. Ndipo matenda a ubongo ndi amodzi amene ankaganizidwa motere chifukwa ankawasowetsa mtendere pozindikira kuti palibe amene ankawamvetsa bwino. Tizindikire kuti m’nthawi imeneyi, kudalibe zipatala. Kale m’nthawi ya Chipangano Chakale, mzimu woyipa unkatanthauzidwa kuti ndi aliyense amene adali ndi matenda amene ankagwira ubongo kapena tinene kuti okhudza maganizidwe a munthu, komanso openga kapena osokonezeka m’bongo (Oweruza 9:23; 1 Samueli 16:14; 18:10).

M’nthawi ya Chipangano Chatsopano, chilankhulidwe cha mizimu yoipa (kugwidwa ndi ziwanda), zinkanenedwa pokamba za munthu yemwe amadwala matenda okhudza ubongo. Kugwirizana pakati pa ziwanda ndi kudwala kukuonetsedwa m’ndime iyi:-

“Ndipo pakudza madzulo anabwera naye kwa Iye (Yesu) anthu ambiri ogwidwa ndi mizimu yoyipa (demons): ndipo Iye anaturutsa mizimuyo ndi mau ake, nachiritsa akudwala onse; kuti chikwaniridwe chonenedwa ndi Yesaya (m’Chipangano Chakale) mneneri, kuti, ‘Iye yekha anatenga zofoka zathu’, Nasenza nthenda zathu” Mateyu 8:16,17).

Choncho apa, zikutanthauzanso kuti zofoka zathuzo ndizo nthenda za ife anthu zomwe zikuyimiranso chimodzimodzi kukhala ndi ‘ziwanda’ kapena ‘mizimu yoipa’. Anthu anaganiza kuti Yesu anali wamisala ndipo kuti n’chifukwa chakuti adali ndi chiwanda; ***“Ali ndi chiwanda nachita misala”***, (Yohane 10:20; 7:19,20; 8:52). Koteru apa, tidziwa kuti iwo ankakhulupirira kuti ziwanda zimayambitsanso misala.

KUCHIZA ODWALA

Pamene anthu ankachiritsidwa, anthu *“ogwidwa ndi ziwanda”* timamva kuti *“ankakhalanso bwino”* – Marko 5:15; Luka 8:35. Izi zikutanthauza kuti ‘pokhala ndi ziwanda’ idaali njira ina yonena kuti munthu sanali bwino m’maganzidwe – mwachitsanzo, anali ndi ‘matenda m’bongo bwake’. Onse amene ‘adali ndi ziwanda’ timamva kuti *“anachiritsidwa”* kapena tinene kuti *“anachizidwa”* (Mateyu 4:24; 12:22; 17:18:- kutanthauza kuti ‘kukhala ndi chiwanda’ ndiko kunenanso mwanjira ina kuti ‘munthu akudwala’ - ndiyo njira ina yonena za munthu kuti akudwala).

M’ndime ya Luka 10:9, Yesu anauza okhulupirira ake makumi asanu ndi awiri kuti apite kutali *“akachize odwala”* zimenedi iwo adapanga. Pobwerera ananena kuti (ndime 17), *“ngakhale ziwanda zimatigonjera ife m’dzina lanu”* ndipo panonso tiona kuti matenda ndi ziwanda sizinasiyanitsidwe m’matanthauzo ayi. Timawerenga kuti nthawi zambiri akuphunzira ndi otsatira ake a Yesu aja ankachiritsa anthu mu dzina la Yesu Khristu ndipo apa ndi chitsanzo china (onaninso Machitidwe 3:6; 9:34).

KUGWIRITSA NTCHITO CHILANKHULIDWE CHA MASIKU AMENEWO

Tafotokoza kale kuti chinali chilankhulidwe chamasiku amenewo pamene tinena kuti munthu ali ndi ziwanda pofuna kutanthauza munthu yemwe wadwala matenda okhudza ubongo, kapena matenda ena alionse omwe anthu sankawadziwa bwino bwino. M’chikhalidwe cha chi Roma ndi chi Greek, anthu ankakhulupirira kuti ziwanda zinkalowa mwa anthu nkukayambitsa matenda m’bongo mwa munthu. Anthu amene akukhulupirirabe izi lero, akubvomereza chikhulupiriro cholakwika ndi chachikunjachi kuti ndi zoono ndicho cholondola kuposa chikhulupiriro mwa Mulungu weni weni wamphamvu’yo. Tikafufuza za mbiri ya Buku Lopatulika, timamva kuti Baibulo linalembedwa m’chilankhulo chimene anthu ankalankhula nthawi imeneyo kuti amve bwino popeza zinkagwirizana ndi kuzindikira kwa anthu a nthawiyo. Chifukwa chakuti Baibulo lidalembedwa m’chilankhulidwe chimenecho, sizitanthauza kuti Baibulo’lo kapena Yesu akubvomereza kuti ziwanda ndi zinthu zamphamvu ina yake ndiponso kuti ndi zamoyo ayi. M’chizungu, liwu loti ‘lunatic’ ponena za munthu amene ali ndi matenda a misala (matenda okhudza maganzidwe a munthu – ubongo). M’chizungumo, liwuli limatanthauza kuti munthu anakhudzidwa ndi mphamvu yochokera

kumwezi (lunar). Kalelo, azungu ankakhulupirira kuti munthu akamayenda usiku kukuwala mwezi, iye ankayangidwa ndi mphamvu yochokera ku mweziyo ndipo kuti zikatero, ankayamba kudwala matenda akumweziwo (lunatic). Lero, munthu aliyense wodwala misala m'chingerezi ndi *'lunatic'*. Izi sizitanthauzadi kuti misala imabwera ndi mweziwo ayi koma kuti chikhulupiriro cha anthu chikutero panthawi imeneyo. Taona kuti pa chitsanzo chimenechi, tikungogwiritsa ntchito mau a nthawi yakaleyo ngakhale kuti ife lero tikudziwa kuti matenda a misala sayamba chifukwa cha mphamvu ya mwezi ayi. Kotero, chilankhulo chakale chikugwiritsidwabe ntchito mpaka lero mofanana ndi maganizidwe a anthu.

Mau atanakhala kuti awerengedwa mzaka 2,000 zikubwerazi – ngati Mulungu atalola, anthu atha kuganiza kuti ife tonse alero tikukhulupirira kuti mwezi ndi umene umabweretsa kapena tinene kuti umayambitsa matenda a misala; Komabe, ife tikuona kuti angalakwitse chifukwa ife tangobwerekera mau'wa kuchokera momwe anzathu akale'wo ankagwiritsira ntchito monga: M'chizungu amatinso 'St. Vitus dance' ponena za mtundu wa gule wina kwaoko, komanso nzodziwikiratu kuti Yesu sanabadwe pa 25 December ngakhale timati tsiku la 'khrismasi' pokamba za tsikuli, maina a masiku msabata lonse nawonso amadziwikanso ndi maina a chipembedzo chachikunja komabe sizitanthauza kuti tonse otchula maina amenewa ifenso ndife akunja ayi; mwachitsanzo, 'Sunday' linali tsiku lopembedza dzuwa (Sun Goddess – 'Sun day'), 'Saturday' ndilo lopembedza 'Saturn' ndipo 'Monday' linali lopembedza mwezi (Moon Day). Izi ndizo zitsanzo zimene zimaonetsa kugwiritsa ntchito mau a nthawi imeneyo ngakhale mauwo ankanthauza zinthu zimene anthu ena sankagwirizana nazo. M'chizungu, liwu loti 'influenza' linkanthauzidwa kuti chinali chinthu choyambitsidwa ndi (influenced by demons) mzimu wonyansa! Pamene Danieli anachita zodabwitsa, iye anatchedwa Belitsazara lomwe linali dzina la fano lina koma linapatsidwa kwa iye chifukwa cha zimene Danieliyo adachita (Danieli 4:19).

Ezekieli motsogozedwa ndi mphamvu ya Mulungu, anagwiritsa ntchito chikhulupiriro chimene anthu anali nacho ndipo anawadzudzula pogwiritsa ntchito chimene iwo ankachidziwadi (Ezekieli 36:13,14). Padalinso chikhaliidwe china chachikunja chimene anthu ankakhulupirira kuti nyanja idali chirombo china chimene anthuwo ankati chidzameza dziko lonse lapansi. Tonse tikamamva izi tikhoza kuona kuti sizidali zoono, koma Baibulo

linagwiritsa ntchito ziphiphiritso zimenezi pofuna kupereka chithunzi thunzi cha mfundo zina zabodza kuti zitsutsidwe ndi chilungamo choyenera cha Mulungu pofotokozerana za chionongeko chfukwa cha machimo. Werengani zitsanzo zina izi pa Yobu 7:12; Masalmo 89:9; Amosi 9:3; Yereimiya 5:22; Habakuk 3:10; Mateyu 14:24; Marko 4:30. Ndipo mwambi wa Assuri unakambapo za chirombo chimene akuti chinali ‘Rahabe’ angakhale kuti ife tonse tikudziwa kuti dzina limeneri linali la mzimayi wina m’Baibulo. Dzina lomweli, linapatsidwa kwa chirombo china cha ku Aigupto pa Yesaya 51:9.

Pozindikira kuti Baibulo ndilo lowuziridwa ndi mpweya kapena tinenenso kuti ndi lowuziridwa ndi Mphamvu ya Mulungu, sitikuona kuti Mulunguyo angachite izi pofuna kutsimikiza kuti zikhulupiriro za chikunja zimenezi zinali zoonza ayi koma kuti ankafuna anthu akhale ndi chidwi poyamba, kenaka chidwi chimene angakhale nachochi, chiwathandize kumvetsa bwino mfundo zofotokozerana zinthu zokhudza maganizidwe amenewa ndi kukonza kwake. Mwanjira iyi, mfundo yaikulu ndiyo yakuti Mulungu Yehova, ndiye ali wa Mphamvu zochulukana. Iye ndi amene atchinjiriza nyanja ndi zina zonse kuti zingaanonge dziko ndi zonse ziri m’menemo. Yehova motero, anakonza zikhulupiriro zolakwika zimene zidalipo panthawiyi kuti ziwongoke ndipo kuti anthu aziwona ubwino pokhulupirira Iye kudzera mwa Mwana wake Yesu Khristu. Baibulo limatitsimikizira kuti zikhulupiriro za makolo ngati zimenezi sizingatitengere kuchipulumutso posatsutsa zomwe anthuwo akukhulupirira ngati siziri zoonza. Kotero, kuli bwino kuwazindikiritsa anthu onse kuti adziwe chikonzero cha Mulungu powerenga Baibulo Loyeralo.

Chitsanzo china ndichomwe chikunena za chiphaliwali komanso mapangidwe owoposa a mitambo yaikulu kuti ndiwo maonekedwe wonga a njoka ya ululu. Izi sizionetsa kuti ndi zoonza ayi, koma kuti Yehova awonetse Mphamvu zake kuti zinthu zonsezi akhoza kuzilandira nazigonjetsa ndipo sizingathe kuperekanso mantha pakati pa anthu ake. Nchifukwa chake ngakhale Yesu anawonetse Mphamvu ya Mulungu pakati pa onse a zikhulupiriro za mizimu yonyansa kudzera mzoziwitsa mosaopa mphamvu zochepe za asing’anga a padziko lapansi. Choncho, sichoyenera kwa mkhristu aliyense kukhulupirira kuti ma ‘demoni’ alipodi. Ife zatitsimikizira kuti Baibulo limangogwiritsa ntchito malankhulidwe a nthawi imene anthu akulankhulira pofuna kutsimikizira mfundo yofunikira pa chipulumutso chathu, ndikutinso tiyeneradi kudziwa kuti palibe mphamvu ina iriyonse yoposa Yehova. Chiuta

ndi amene adziwa za mayesero athu popeza mphamvu zonse padziko analenga ndi Iye. Moteronso lero, kuti bvuto liyambike mwaife, tingathe kumvetsa bwino m'mene tingaligonjetsere chifukwa tikhutira ndi kumvetsa chiyambi mpakana magwero ake. Choncho, tidzayesetsa kuyikapo luntha mbali yathu kuti tilandire mphototho yochokera kwa Iye Wamphamvuyo.

Tiyeni tsopano tione zitsanzo zochokera m'Chipangano Chatsopano motere:

- ✓ A falisi anam'nyogodola Yesu kuti ankachita zozizwitsa ndi mphamvu ya Beelzebule limene linali dzina la fano. Yesu anawayankha kuti, ***“Ndipo ngati ine ndimatulutsa ziwanda ndi mphamvu yake ya Beelzebule, ana anu amatulutsa ndi mphamvu ya yani?”*** (Mateyu 12:27). Tikawerenga 2 Mafumu 1:2, akutiwuzwa momveka bwino kuti Beelzebule anali mlungu wabodza wa Afilisiti. Yesu sanafune kuwauza ichi kuti iwo adziwerengere okha pa 2 Mafumu 1:2 ayi. Iye anayankha ngati kuti Beelzebuleyo alipodi ndikuti alidi mlungu ncholinga chakuti anthu amene ankalemekeza Beelzebule uja, asakhumudwe koma kuti nawonso amvetse pamodzi ndi onyozawo za Uthenga Wabwino wa Yesu'wo yense payekha payekha. Motero, anthu onsewo anatolapo phunziro lalikulu pomaliza pake nazindikira zoonza zokha zokha za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu.
- ✓ Machitidwe 16:16-18 ndi mau amene analembedwa ndi Luka mowuziridwa ndi mpweya wa Mzimu Oyera; ***“..anakumana ndiife namwali wina amene anali ndi Mzimu wambwebwe..”*** Apanso tiona kuti m'bobo (mbwebwe) linali dzina la fano lomwe anthu ankapembedza m'chirumika choyambirira ndipo ena ankalitchulanso kuti napolo. Tiyenera kuzindikira kuti fano limeneri kotero, silinali mlungu weni weni komabe Luka anagwiritsa ntchito chikhulupiriro ndi chizindikiro chimenechi kuti anthu amene ankadziwa ichi amvetse bwino mfundo yakeyo. Moteronso, Uthenga Wabwino siumanena kuti Yesu ankachotsa mizimu imene kudalibe ayi koma kuti ankachiza matenda (ponena kuti wachotsa mizimu yonyansa ngati m'mene ankalankhulira anthu ambiri nthawi imeneyo).
- ✓ Luka 5:32 akuti, ***“sindinadza Ine kuyitana olungama,”*** Apa tikhozanso kuona kuti Yesu ankatanthauza kuti 'sanadze kudzaitana anthu amene amadziona ngati kuti ali olungama'. Tingazindikire bwino pamenepa komanso kumvetsa kuti Yesu anagwiritsa ntchito chilankhulidwe chawo cha anthu amene ankamufunsa momukola aja

powatsutsa maganizidwe awo pakati pa anzawo mchilankhulo chimene iwo ankachidziwa. Anthuwo sindiye kuti analidi olungama monga Yesu ananenera ayi. Luka 19:20-23 tiona kuti Yesu akugwiritsanso ntchito chilankhulidwe chimene sichinali choona ndipo sanafune kukonza maganizidwewo pokamba za fanizo la matalente lija ayi.

- ✓ Baibulo nthawi zambiri limakamba za dzuwa kuti *'limatuluka'* ndi *'kulowa'*. Umu ndim'mene anthufe timalankhulira ngakhale panopa koma sikuti dzuwa limatulukadi ndi kulowa ayi. Ngakhale a *'science'* (ophunzira za chilengedwe cha zinthu) amakana maganizidwe amenewa koma Yesu sadafune kutero ayi. Nchifukwa chake matenda ankakambidwanso ngati kuti ndi ma demoni popeza nthawi imeneyo munthu akadwala, chilankhulidwe chinali chotero. Machitidwe 5:3 akunenanso za m'mene Ananiya ananamira pamaso pa Mzimu Oyera. Tikaona mofatsa, sichoyenera kunamiza Mzimu Oyera ayi, nchifukwa chake Ananiya ndi mkazi wake timamva kuti onse analangidwa naafa nthawi yomweyo.
- ✓ Zitsanzo zina m'Baibulo pa zilankhulo za masiku amenewo pa mutu womwewu zikupezeka pa Yobu 2:4 pamene tiwerenga kuti ***"khungu kulipa khungu"*** ponena za malipiro pamene munthu alakwira mzake kotero ayenera kulipira chofanana ndi chimene walakwiracho. Tionanso kuti mwamuna wa chiwerewere pa Deuteronomo 23:18 akutchedwa *'galu'*, mnjira yomweyo.
- ✓ Ayuda m'nthawi ya Yesu ankaganiza kuti iwo ndiwo anali olungama chifukwa chakuti anabadwa mwa Abrahamu. Choncho, Yesu sanawatsutse ayi koma anawatchulanso olungama. (Mateyu 9:12,13), nati ***"Ndidziwa kuti muli mbeu ya Abrahamu"*** (Yohane 8:37). Titaonetsetsa apa tikupeza chinthu chimodzi chodziwikiratu ndicho kuti, Yesu sanakhulupirire kuti a Yuda aja anali a chipembedzo choyenera, ndipo kuti analidi olungama monga Abrahamu! Tikawerenga Yohane 8:39-44 tiona momwe Yesu anawaunikirira kuti iwo sanali ana a Abrahamu monga ankanenera pamenepa poyerekeza ndi zochitika zawo. Anachita izi pobvomereza malankhulidwe awo poyambirira, kenaka anawatsutsabe powawunikiranso kudzera mchilankhulidwe chawo chomwecho. Tsopano taonetsa kuti iyi idali njira imene Mulungu ankatsata powunikira anthu akunjira pa nthawi ya Chipangano Chakale. Ndipo Yesu anatsatanso njira yomweyo m'Chipangano Chatsopano. Zozizwitsa zimene anachita Yesu pakati pa

makamu zinaonetseratu kuti matenda anadza kuchokera kwa Mulungu poonanso kuti anali Mulungu yemweyo amene anatha kuchiza nthenda zonsezo ndi Mphamvu zimene ali nazo.

- ✓ Paulo analankhula za olemba a chi Greek kuti malembo awo sanaonetse chikhulupiriro chopezeka m’Baibulo. Choncho, anawachenjeza anthu kuti sayenera kutsata chiphunzitso chabodzachi (Tito 1:12; Machitidwe 17:28). Komabe popitiriza ulendo wake, Paulo anapezanso malo ena pomwe paguwa lake padalembedwa kuti, **“Kwa Mulungu wosadziwika”** mwachitsanzo; akanatha kukhala Mulungu wachikunja komanso fano la mlungu amene anthu onse aku Atene anamuyiwala nasiya kumpembedza. M’malo mowadzudzula pachipembedzo chawo chonamacho, Paulo anawayamikira poyamba kunena zimene iwo anadziwa kale zogwirizana ndi mlungu wosadziwika uja. Motero, chikunja chawo chinawathandiza komanso kuwayandikiritsa chifupi kuti iwo paokha, adziwe choonadi cha uthenga wabwino ndi Mulungu weni weni m’modzi yekhayo amenenso ali wamphamvu zochulukana (Machitidwe 17:22,23).
- ✓ Chitsanzo china cha Paulo chiri pa Aefeso 2:2 pamene alankhula za **“mkulu wa ulamuliro wamlenga lenga”**. Ichi, chinali chikhulupiriro cha anthu aku Greece kuti panali mphamvu yochokera mlenga lenga yomwe inali ndi ulamuliro umene iwo ankayenera kuwumvera. Paulo akunenetsa kuti ngakhale iwo anakhala panso paulamuliro wa mphamvu imeneyi, ayenera kusintha ndikutsata ulamuliro wa choonadi chifukwa ulamuliro wao woyambawu ndiwosayenera. Iye ananena kuti ulamuliro waowu ndiwogwira ntchito mthupi koma ulamuliro watsopanowu, upereka mphamvu ya dongosolo loyenera la choonadi. Paulo sananyoze ulamuliro woyambawo ayi chifukwa ndi umene anthu ambiri ankawulemekeza kotero, anagwiritsa ntchito chikhulupiriro cholakwikacho pofuna kuwaphunzitsa chikhulupiriro cheni cheni chimene chili choonadi cha Yesu Khristu.
- ✓ Pa Machitidwe 28:3-6 tiwerenga zamomwe Paulo analumidwira ndi njoka yaululu komanso yolusa pa mkono wake. Chifukwa chaichi, anthu anaganiza kuti Pauloyo anali wakupha popeza anapeza tsoka lotere. Munthu akapezeka ndi tsoka lotere, zikhulupiriro za anthu nthawi imeneyo zinali zakuti munthuyo ndi woyipa mtima komanso wakupha. Choncho, Paulo anamuganizira mwanjira imeneyi. Tikhoza kuona kuti maganizidwe otere sanali owona ngakhale Paulo sanafune

kuwatsutsa anthu aja. Iye anawaphunzitsa pochita chinthu chimene chinali chozizwitsa pakati pawo. Chinthu chimenechi chinaonetsa chikhulupiriro chodabwitsa ndinso choonadi cha Paulo mwa Khristu Yesu. Molimba mtima, Iye anayiponya pansi mwamphamvu njokayo ndipo panthawiyi, nkuti njokayo isanamulume. Anthu sanakhulupirire kuti zoterezi zingachitike pamaso pawo malingana ndi m'mene zinaliri zikhulupiriro zawo zakale.

- ✓ Tikawerenga zozizwa za Yesu Khristu, tiona kuti zinkachitika ncholinga chakuti ziwonetse zikhulupiriro zawo anthu aja monga kunena za mizimu yonyansa, kuti sizinali zoyenera ndi zoono pamaso pa Mulungu weniweni wa Israeli. Yesu pankhani iyi sananena molunjika ayi chifukwa sanafune kuwakhumudwitsa anthuwo koma kuti anakamba ngati kuti zikhulupiriro zimene anthu anali nazozo zinali zoono. Nchifukwa chake pa Luka 5:21, ngakhale a Yuda ankanama kuti Yesu ananyoza Mulungu, kutinso ndi Mulungu yekha angatikhulukire machimo athu osati Yesuyo ayi; Iye sanafune kukangana nawo powatsutsa ayi. Mosataya nthawi, anachita zozizwitsa zimene zinaonetseratu poyera mfundo zake kotero, a Yudawo anatsutsikanso.
- ✓ Nzodziwikiratu apa; Yesu anaonetsa kuti ntchito zathu ngati a khristu zimakweza choonadi cheni cheni kuposa nkambakamwa za anthu. Yesu Khristu sanatsutsepo zabadza zonse zimene anthu ankamunenera ndipo moteronso, sanatsute zinthu zoyipa ziri zonse zimene anazona m'malamulo a Mose zomwenso sizikanabweretsa chipulumutso koma m'malo mwake, amangochita chinthu china chake monga; kuchiza wodwala patsiku la Sabata, tiona kuti izi ndizimene zinali zoyenera pa chipulumutso. Nthawi ina yake atamunamizira kuti anali msamaliya, Yesu sanakanepo chiri chonse ayi (Yohane 8:48,49 cp.4:7-9) ngakhale kuti kukhala m'Yuda chinali chinthu chofunikira kwambiri pa ndondomeko ya Mulungu imene a Yudawo ankayidziwa ngati chofunikira koposa pa chipulumutso cha munthu (Yohane 4:22).
- ✓ A Yuda anamunena dala Yesu Khristu ncholinga chakuti amutayitse chikhulupiriro chake naati; “...*anadziyesera wolingana ndi Mulungu*” (Yohane 5:18), Yesu sanataye nthawi nkukana nkhanayi; Iye anangowakumbutsa anthuwo kuti ankachita zozizwitsa powonetsa kuti ngakhale anali munthu, ankachita izi motumidwa ndi Mulungu kotero, munthu wotumidwa sangalingane ndi womutumayo ayi. Ndipo kutinso zozizwitsazo zinkaonetsanso kuti zikhulupiriro za mizimu yonyansa

zinali zabodza. Pankhani ya munthu wopuwala amene anachizidwa pa thamanda la Betesda, akutiphunzitsa kuti chikhulupiriro chimene a Yuda anali nacho chonena kuti nthawi ya Paskha m'ngelo ankakhudza thamanda la Betesdalo, nayikapo mphamvu ya machiritso sizinali zoonza. Yesu m'malo mwake, sanatsutse ayi, koma anangomuchiza munthuyo atalephera kale kuchira pamene anakhudza madzi a pa thamandalo kwa nthawi yaitali. Izi zinaonetsa mphamvu yaikulu imene Yesu Khristu anali nayo ngakhale a Yudawo sanathe kuyiona.

- ✓ Pa 2 Petro 2:4 timawerenga kuti anthu ochimwa adapita ku ndende (hell, tartarus). Mau oti **Tartarus** anali mau onena za malo amene anthu nthawiyo ankakhulupirira kuti anali pansu kapena tinene kuti ku midima. Koma Petro sanawatsutse anthuwo kuti pansu padziko lapansi kulibe malo amenewa koma kuti anthu paokha ankangoganiza kuti malowa alipo. M'malo mwake, anagwiritsa ntchito mau omwewo a bodzawo ngati chizindikiro cha chiwonongeko kwa anthu ochimwa. Mnjira imeneyi, Yesu anagwiritsanso ntchito mau oti '**Gehena**' (onani phunziro 4.9) ngakhale kuti malo'wa sanali malo otanthauza za chilango cha anthu oyipa koma chitsanzo chabe.

KODI MIZIMU YONYANSA (DEMONS) IMAYAMBITSADI MATENDA?

Onse amene amakhulupirira kuti mizimu yoipa (demons) iripodi ndipo kuti imayambitsa matenda ayenera kudzifunsa kuti: '**Ine ndikadwala kodi matendawa amayambika chifukwa cha mizimu yonyansa?**' '**Nanga nchifukwa chiyani matenda amene adalembedwa m'Chipangano Chatsopano kalelo kuti anali matenda a mizimu yoipa amachizidwa lero lino?**' '**Kodi ndi zoonza kuti milungu imeneyi imayenda yenda nkumayambitsa matenda kapena zoyipa pakati pathu?**' Zindikirani kuti ena mwa matenda akuchizidwa lerowa amenenso nthawi yapitayo ankabvuta kwambiri kuwachiza ndiwo malungo. Anthu ambiri muno mu Africa amaganiza kuti malungo amayambidwa chifukwa cha mizimu yonyansa. Ife lero tiri ndi mwayi chifukwa tikudziwa kuti izi sizili choncho. Tikudziwanso kuti munthu akagwidwa ndi malungo, amachira akamwa mankhwala otchedwa **kwinini** ndi ena otero. Choncho, sindikhulupirira kuti mizimuyi imathawa ikaona **kwininiyo** ayi. Ena mwa matenda odziwika bwino amenenso anthu ankati ndi obwera ndi mizimu ndiwo kafumbata (**Tetenasi**) komanso khunyu

ndipo matenda onsewa lero lino amachiritsidwa bwino bwino ndi mankhwala amene tsopano alipo.

Tsiku lina m'bale wina wa ku Uganda anafotokoza kuti anthu ambiri kwaoko ankakhulupirira zoti malungo amayamba chifukwa cha mizimu yoipa. Pamene anazindikira kuti pali mankhwala omwe amachiritsa matendawa, adasiya kukhulupirira zonena kuti matendawa ndi a mizimu. Komabe, malungo ogwira bongo ankawatengabe kuti ndi matenda obwera chifukwa cha mizimu. Tsiku lina dotolo anabweretsa mankhwala a malungowa koma anthu odwala kumeneko ankawakana chifukwa iwo ankafunitsitsa mankhwala okhawa amene angathamangitse mizimuyo. Dotoloyo anangobwerera nawo mankhwala aja. Kenaka iye anaganiza zopitanso kumaloko. Ulendo wina dotolo uja anabweretsa mankhwala omwe aja nawanamiza odwalawo kuti wabweretsa mankhwala othamangitsa mizimu yonyansayo. Anthu aja analandira naamwa mankhwalawo ndipo nthawi imeneyi anachira patatha masiku awiri. Apa tionanso kuti dotolo'yu anadziwa kuti anayenera kulankhula chilankhulidwe chimene anthuwo ankachidziwa ndinso ponena mzinthu zimene iwo ankazikhulupirira. Akanapanda kutero, odwala aja sakanalola kumwa mankhwala aja ndipo motero, akanafa nawo matendawo. Iye anaonetsa njira yomwe Yesu Khristu ankachita ngati dotolo wamkulu mzaka 2,000 zapitazo.

MPATUKO 17: UMFITI

Mpatuko uno walembedwa pofuna kuthandiza anzathu aku Africa kuno komanso kumayiko ena padziko lapansi kumenenso anthu amakhulupirira za umfiti. Onse ophunzira za Baibulo, amadziwiratu kuti chikhulupiriro cha umfiti ndi ung'anga mu Africa muno nthawi zonse sizigwirizana ndi chikhulupiriro cha m'Baibulo. Tikudziwa kuti ung'anga nthawi zambiri umathadi kuchiritsa matenda pa mitengo yozizira koma, tiyenera tidziyese tokha ndi mlingo wa Baibulo tisanapite kumalo amenewa nkuona ngati nkoyenera kukapeza chithandizo.

ZIMENE A MFITI AMACHITA

Choyamba, tiona kuti a mfiti ndi a sing'anga amakonda kuchita zinthu zawo m'malo ndi nthawi zobisika komanso mwachinsinsi. Izi zikusiyana koposa ndi m'mene a zachipatala ndi a science (ochiza ndi ofufuza fufuza za umoyo wa zinthu) amachitira ntchito yawo. Anthu ambiri ochizidwawo kawiri kawiri sizidziwika kweni kweni kuti achizidwadi kapena ayi. Tikaonanso, asing'anga amenewa akupezeka m'malo ochepa padziko lonse lapansi lino ndipo kuti kumayiko kwina kulibiretu.

Ena ainu amene mungayesedwe kuti mupite kukaona a ng'anga amenewa, muyenera mudzifunse nokha kuti; *“Kodi ndizoona sing'angayo amachizadi molongosoka komanso mogwirizana ndi choonadi?”* Buku la Deuteronomo 13:1-3 timawerenga zina zimene zingatipatse mphamvu zapadera: Ana a Israeli analangizidwa kuti ngati sing'anga ali ndi chizindikiro kapena kuti akhoza kuchita chozizwitsa chimene sichikugwirizana ndi zimene Mulungu amafuna, iwo ayenera asamubvomereze, amukane ndithu. Nzowonekeratu kuti a sing'anga sakugwirizana ndi zimene Mulungu amatiphunzitsa m'Baibulo kotero, sityenera kuwakhulupirira kuti ali ndi mphamvu zeni zeni chifukwa ife timadziwa kuti wamphamvu zoposa zonse ndiye Mulungu yekha basi (Aroma 13:1; 1 Akorinto 8:4-6).

Chachiwiri, zikuoneka kuti ambiri mwa a sing'angawa amachiza pongoyerekeza chabe zimene odwalawo amaganiza ndi m'menense amakhalira mwachitsanzo, munthu odwala uja amangowumirizidwa kubvomera kuti wachira chifukwa chotopa ndi mafunso amene amangofuna kuthana nawo pobvomereza kuti iye wachira pamene nthawi zambiri sinziri chomwechi. Anzathu ophunzira za maganizidwe (psychologists), amatiwuzwa kuti ngati munthu aganiza kwambiri atha kupenga komanso mwina kudwala zironda zam'mimba kuphatikizapo mutu. Ngati munthu oganiza kwambiri uja angadzisangalatse mokwanira mwanjira ina, kusangalalaku, kumapangitsa kuti munthuyo ayiwale zimene akuganizazo ndipo ululu wa matenda uja umatha niuzizira. Motero, a sing'anga amathanso kutinamiza mwanjira imeneyi kuti maganizidwe athu amasuke ndipo kuti tikhale ngati tiri bwino pongoganizira. Chifukwa chosamvetsa bwino maphunziro amenewa, titha kuona ngati kuti tikuchira ndi mankhwala a sing'anga pamene siziri choncho koma kuti ululu wangochepe chabe.

GWERO LENI LENI LA MPHAMVU

Timadziwa mopanda chikayiko kuti mwini mphamvu yonse padziko lapansi ndiye Mulungu Yehova. Mphamvu zonse zabwino ndi zoyipa zichokera kwa Mulungu. Matenda ndi zina zonse zoyipa koma osati umfiti kotero, amabweretsa ndi Chiuta monga tikuwerenga m'Baibulo (Yesaya 45:5-7; Mika 1:12; Amosi 3:6; Eksodo 4:11; Deuteronomo 32:39; Yobu 5:18). Tikawerenga ndime zimenezi tiona kuti ndi Mulungu yekha amene angatiwunikire bwino pamene tadwala kapena tapeza mabvuto osiyana siyana. Kotero, tiyenera kupemphera kuti Iye Mwini zonsezi azitiyangata ndi dzanja lake limenenso limatha kubweretsa ndi kuchotsa zipsinjozi. Tadzimvera kuti Yehova amatha kutichotsera choyipa nabweretsa chabwino popeza Chiuta ndi gwero la zonse ndipo amadziwadi magonero a zonsezo. Kotero, tikapita kwa a sing'anga amaoneka ngati kuti a sing'angawo ndi amene ali ndi mphamvu zogonjetsera zonsezi kuposa mphamvu za Mulungu. Tiyeni tisalemekeze makopedwe a sing'anga omwe sangaponse mphamvu ya Mulungu chifukwa Yehova angathe kubweretsa matenda nawachotsanso. A sing'anga iwonso, timaona kuti akadwala amatha kufa, kutanthauza kuti nawonso amayilephera mphamvu ya Mulungu chifukwa matendawo amachokera kwa Chiuta kotero, mnzeru zawo zokha, sangathe kudzichiza kapenanso kuchiza anzawo. Baibulo likutitsimikizira ndi kutilimbikitsa kotero, kuti tikhulupirire Yehova mu zonse popeza Iye ali Mwini zonsezo pansu ndi kumwamba. Mulungu sakondwera ngati tikhulupirira za a sing'anga ndi a mfiti.

Munthu amene amakhulupirira ndi kulemekeza a sing'anga akwiyitsa Mulungu chifukwa kukhala ngati iye akuderera Yehovayo. Ana a Israeli anapembedza mafano ngakhale kuti ankalemekezanso Yehova wao. Izi zinamukwiyitsa Chiuta ndipo mpaka anawauza kuti iwo sayeneranso kutchulidwa ana ake (Deuteronomo 32:16-24). Pokhapokha titayika chikhulupiriro chathu pa Yehova Mulungu wathu, sitingayenerazedwe kukhala ana ake a Mulungu. Tikhoza kukwaniritsa ufulu umenewu wokhala ana a Mulungu ngati tisiyadi kulambira milungu ina, mafano komanso mizimu yonyansa. Israeli anakanidwa chifukwa cha mbiri yawo yosayenera pochita zinthu zoyipa ngati zimenezi ndipo mwaichi, nkhani imeneyi ya mafano inalembedwa kuti ife titengapo phunziro. Sitiyeneradi kulumikizana nawo onse amene amakhulupirira za milungu ina ndi mphamvu za mizimu yoipa.

“...pakuti chilungamo (kuwala) chigawana (chilumikizana) bwanji ndi chosalungama? Kapena kuunika kuyanjana bwanji ndi mdima? ...Kapena wokhulupirira ali nalo gawo lanji pamodzi (ndi) wosakhulupirira?...Pakuti ife ndife kachisi wa Mulungu wamoyo...ndipo ndidzakhala Mulungu wao ndi iwo adzakhala ana anga amuna ndi akazi...Chifukwa chake tulukani pakati pawo ndimkhale opatulidwa” (2 Akorinto 6:14-16).

Tikadzapatula ndi kuyesetsa kukana zinthu zonse zonyansa pamaso pa Mulungu, Yehova Mwini atitsimikizira ife kukhala ana ake. Moteronso, Mulungu amene ali atate wathu adzatiyanjanitsa natitchinjiriza chakwayipa china chirichonse ngakhale kumatenda kumene. Kodi sichinthu chanzeru kukhulupirira Iye kotero kuti Chiuta adzatisamalire?

Tiyenera kuzindikira kuti a mfiti amakhala ndi mphamvu kwa iwo okhawo amene amakhulupirira mwa amfitiwo. A mfiti amanamiza anthu awo owakhulupirira nchifukwa chake, ngakhale kale mnthawi ya Farao ndi Nebukadnezara, a mfiti ankachita zinthu zosiyana siyana powonanso chikhulupiriro chimene Farao ndi Nebukadnezara anali nacho mwa amfitiwo. Tiona kuti pamene Mulungu anatengapo mbali pofuna kuwonetsa kufooka kwa amfitiwo, mphamvu zawo zidachepa panthawiyo ndipo ulemu umene ankapatsidwa pamaso pa anthu udachoka. Chimodzimodzinso, zinali choncho pamene Baraki anakhulupirira mphamvu za Balamu potemberera anthu. Koma Balamu amene adali mthakati wamphamvu zake, anazindikira kuti mphamvu zake sizinkagwiranso ntchito pa ana a Isreali (Numero 22:6). Izi zikuonetseratu kuti mphamvu ya umfiti iriyonse ili chabe pa ana ndi anthu okhulupirira Mulungu.

UMFITI MOGANIZIRA ZIMENE BAIBULO LIMANENA

Ambiri a ife takhala tikudziwa kuti kudziko kuno kuli a mfiti ndi a sing’anga. Anthu ena akhala akupita kwa a sing’anga kuti akapeze machiritso pa nthawi imene iwo akudwala ngakhale ali akhristu. Pamene ife tipita kwa a sing’anga, zimatanthauza kuti tiri ndi chikhulupiriro chokwanira mwa a sing’angawo. Mwaichinso, ngati timadzitchinjiriza mwa amfiti, ndiye kuti timakhulupirira kuti amfitiwo ali ndi mphamvu zochuluka ndipo kuti mnjira imeneyi, timayiwaladi Mulungu wathu Namalenga. Zikafika apa, zinthu zonse mwa ife sizingayende bwino ndipo chiyembekezo chatu chabwino chochokera kwa

Yehova chimazimira pamenepa. Kutsogolo kwa moyo wathu kotero, kukhala mdima wokha wokha. Tikakumbutsana za Farao, Baraki ndi Nebukadneza munga tafotokoza kale mmwambamu, tiona kuti nkosayenera kwa mkhristu aliyense kupeza chithandizo kwa amfiti kapenanso a sing'anga. Tingaonenso kuti sikuyenera mkhristu kupempha chithandizo chirichonse kuchokera kwa a sing'anga chifukwa a sing'angawo alibe mphamvu zimene zingaponse mphamvu ya Yehova. Mkhristu ndiye munthu wa Chiuta ndipo ndi mwana wa Mulungu munga timawerenga. Tonse timayenera kuzindikira kuti mayitanidwe athu ngati akhristu mu ubatizo oyenera amatitsimikizira kwathunthu kuti tiyenera tisunge chikhulupiriro chathu mzonse pa Iye.

Umfiti ndi *“ntchito za thupi”* munga Paulo akutilangiza pa Agalatiya 5:19 motere: ***“Ndipo ntchito za thupi zionekeera, ndizo dama, chodetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano...”***

Langizo lina likupezeka pa Deuteronomo 18:10,11; Eksodo 22:18 mmalamulo a Mose, pamene tikuwerenga kuti a mfiti onse, otamba onse, a masenga onse komanso owotcha ana awo pa guwa ngati nsembe yopsereza, amasenga ndi a dama onse ayenera kuphedwa. Apa tiona kuti angakhale ena onse amene ankatsamira pa a sing'anga ankayenera kuphedwanso. Motero, mChipangano Chatsopanochi, chilango chake ndicho kukanidwa mu Ufumu wa Mulungu.

Ngati munthu afuna kupeza bwino, sayenera kufuna funa chithandizo kwa a sing'anga. Tisanachite chinthu chirichonse, timayenera tiyike patsogolo pathu Yehova Mulungu wathu kuti atiunikire mzonse. Tizidzifunsa ngati chinthu chimene tifuna tichite nchobvomerezeka pamaso pa Mulungu. Umfiti pamaso pa Mulungu, umatanthauza *“kuukira”* munga timawerenga pa 1 Samueli 15:23. Tiwerenganso pa Deuteronomo 32:16-19 kuti kukhulupirira za umfiti kumakwiyitsa Mulungu Yehova. Ana a Israeli anauzidwa kuti agonjetse komanso athamangitse anthu aku Kanani chifukwa chakuti anthuwo ankakhulupirira napembedzanso mafano. Kupembedza fano ndiko kupembedza kosayenera pamaso pa Chiuta. Komabe, timva kuti mmalo mothamangitsa anthuwo, ana a Israeli anatsatira chipembedzo chonyansacho osachikana nayanja Mulungu wao (Deuteronomo 18:9-14). Ifenso ngati Israeli watsopano, sitienera kuchita zimene ana a Israeli anachita ayi, koma kutsata chilongosoko mchoonadi.

Mulungu azititchinjiriza mzipsinjo zosiyana siyana mmasiku ano owawa, a mdima kuti tonse a mitundu ndi ana ake eni eni a Isreali okhala ndi

chikhulupiriro tikalowe mu ufumu wake mchilungamo cha ulemerero wake (2 Atesalonika 2:10-17).

“..popeza chikondi cha choonadi sanachilandira, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo chifukwa chake, Mulungu atumiza kwa iwo machitidwe a kusoheretsa, kuti akhulupirire bodza;...Koma tiyenera ife tiziyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu, abale okonedwa ndi Ambuye, mulandire chipulumutso mwa chiyeretso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi; kumene anayitanako inu mwa Uthenga Wabwino wathu, kuti mulandire ulemerero wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Chifukwa chake tsono, abale, chirimikani, gwiritsitsani miyambo imene tinakuphunzitsani, ...Ndipo Ambuye Wathu amene anatikonda natipatsa chisangalatso chosatha ndi chiyembekezo chokwana mwa chisomo, asangalatse mitima yanu, nakhazikitse inu mu ntchito yonse ndi mau onse abwino”

MPATUKO 18: CHINACHITIKA NCHIYANI MMUNDA WA EDENI?

Genesis 3 vs.4-5 *“...Ndipo njokayo inati kwa mkaziyo; Kufa simudzafa ai; chifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoyipa”*

MMENE ANTHU AMBIRI AMANENERA:

Anthu ambiri amanena kuti njokayo idali mngelo amene anachimwa pamaso pa Mulungu koteru, anachotsedwa nathamangitsidwa kumwamba kudza panso pano ndipo kutinso ndi amene lero amatchedwa “Satana”. Moteronso, Satana atathamangitsidwa ndi Mulungu, anathawira panso pano ncholinga choti anthu amene anali olungama pamaso pa Yehova awayese koteru, iwo achimwe namuyesa Heva ndipo kuti iwo anachimwadi.

NDEMANGA:

1. Nunsuyi, siinatchulepo za “njoka”. Mau oti “Satana” ndi “Mdierekezi” sanalembedwepo pa ndime imeneyi komanso m’buku lonse la Genesis. Tonse timadziwa kuti njoka zimapezeka pakati pathu ndipo kuti pamene njokayo inapezeka mmunda wa Edeni, sichingakhale chinthu chachilendo popeza kunalinsu tchire monga lero lino tili ndi matchire. Moteronso, pamene tiona njoka, sitinganene kuti ndiyo Satana monga ena amakhulupirira kuti njoka ya mndime imeneyi ya Genesis 3 idali Satana.
2. Njoka siyinatchulidwepo kuti ndiyo mngelo m’Baibulo.
3. Koteru, nchosadabwitsa kuti Buku lonse la Genesis silikambapo zomanena kuti padali mngelo amene anathamangitsidwa ndi Mulungu kuchokera kumwamba nathawira padziko lapansi lino.
4. Tchimo limabweretsa imfa pakati pathu (Aroma 6:23). Ndipo tidziwenso kuti Angelo samafa (Luka 20:35-36), choncho, zikutanthawuzanso kuti Angelo sangachimwe. Mphotho ya chiyero ndiyo kufanana ndi Angelo amenenso samafa koteru, oyera mtima samafanso (Luka 20:35-36). Angelo atachimwa, ndiye kuti oyera mtima onse akhoza kuchimwa ndipo motero, ayenera kufa ndithu, kutanthauzadi kuti sangalandire moyo wosatha.
5. Onse okhudzidwa (amene anatenga mbali) pa tchimo la munthu mmunda wa Edeni anali awa: Mulungu, Adamu, Heva ndi Njokayo. Palibenso wina amene watchulidwa pamwamba pa amenewa ayi. Choncho, palibe umboni wina uliwonse owonetsa kuti chinthu china chinalowa mu mtima mwa njoka kuti inyengerere munthuyo ayi, Baibulo silikutero. Paulo akunena kuti njoka “inanyengerera Heva ndipo kuti inatha kutero chifukwa inali yochenjera ” (2 Akorinto 11:3). Ndipo Mulungu anayiwuza njokayo: **“Chifukwa kuti wachita ichi”** (Genesis 3:14). Ngati Satana ankagwiritsa ntchito njokayo, chifukwa chiyani sanatchulidwepo mndime zimenezi ndipo, bwanji Mulungu sanatembererensu Satanayo popeza tikuona kuti onse amene anatengapo mbali pa tchimo la mmunda wa Edeni onse anatembereredwa?
6. Adamu anamunamizira Heva nanena kuti ndi amene adamuchimwitsa **“...anandipatsa ine za mu mtengo”** (Genesis 3:12). Heva naye sanalekerere ayi koma kunamiziranso njokayo **“...njoka inandinyenga ine ndipo ndinadya...”** (Genesis 3:13).

Tsopano onani kuti njoka ija siinanamizire mdierekezi ayi, iyo siinadandaulenso kapena kukana ayi.

7. Tikhoza kutsutsa kuti njoka sizilankhula ngakhale lero lino siziganiza monga njoka ya mmunda wa Edeni – kumbukirani kuti (a) Bulu nthawi ina yake analankhula ndipo anapempha munthu (Balamu) kuti aganizire bwino “*...koma anadzudzulidwa pa kulakwa kwache m'neneriyo*” (2 Petro 2:16) ndi (b) Ndipo njokayo “*..inali 'yochenjera kwambiri' yoposa zamoyo zonse za mthengo zimene anazipatsa*” (Genesis 3:1). Motero, temberero limene Mulungu anapereka kwa njokayo, tiona kuti ndi lomwelo linachotsa mphamvu yolankhulana ndi anthu monga Adamu ndi Heva mwanjokayo.
8. Mulungu ndi amene analenga njoka (Genesis 3:1); palibenso chinthu china chamoyo chomwe chinasandulika kukhala njoka kapena kulowa mwa njokayo ndipo kuti chinatchedwa ‘Satana’ poyambapo ayi. Ganizo loti munthu kapena chinthu chingalowe mwa chinthu china kapena munthu wina nkumasintha umoyo wa munthuyo kuti azichita zinthu zatsopano silingakhale ganizo lowona maka maka pamene tiwerenga Baibulo mozama. Tiyeni motero, tizikumbukira nthawi zonse kuti tchimo linadza padziko kudzera mwa munthu osati chinthu china ayi (Aroma 5:12). Njokayo choncho, inali yamoyo, yodziwa kulankhula mwachilengedwe chake choyambacho ndipo koteru, inalibe udindo wina uliwonse kwa Mulungu. Munthu ndi amene adali ndi udindo kwa Mulungu Yehova chifukwa anawuzidwa zinthu zimene iye akanayenera kumachita pamene iye analengedwa pa dziko lapansi.

Ena amanena kuti njoka ya mu Genesis 3 ija ikufanana kwambiri ndi ntchito imene inagwiridwa ndi ‘Mkerubi’. Tiona kuti liwu la chi Greek limene linamasuliridwa kuti ‘mkerubi’, silikugwirizana mpang’ono pomwe ndi tanthauzo la njoka ya mu Genesis 3. Liwu la chi Hebra la ‘Seraphim’ likutanthauza kuti ‘owopsayo’ ndipo lidatanthauzidwa kuti ‘njoka yoopsa’ pa Numero 21:8 koma sizitanthauzira liwu la njoka ya mu Genesis 3. Liwu la chi Hebra loti ‘mkuwa’ ndi limene likufanana mmatanthauzo ndi liwu loti ‘njoka’ mu Genesis 3. Mkuwa ukuyimira ‘tchimo’ (Oweruza 16:21; 2 Samueli 3:34; 2 Mafumu 25:7; 2 Mbiri 33:11; 36:6), moterodi, njoka ikuyimira ‘tchimo’ koma sanakambepo kuti liwuli limayimiranso za ‘mngelo wochimwa’ monga ena amanenera kuti mngeloyo anaponyedwa pansu pano.

ZIMENE NDIMEYI IKUNENA:

1. Tiyenera kumvetsa mopanda chikayiko kuti chilengedwe cholembedwa m’Buku la Genesis mmitu yoyambirirayo ndi zinthu zimene zinachitikadi ndithu. Ndipo mwaichi, njokayo inalidi njoka yeni yeni imene ngakhale lero timayidziwanso bwino kuti imakwawa monga mwa temberero limene Yehova Namalenga anaperekadi kwa njoka yoyamba ija (Genesis 3:14). Mndondomeko yomweyi, munthu wamwamuna ndi wamkazi timawaonanso akukhala nakwaniritsa matemberero amene Chiuta, anawapatsa kwa munthu oyambayo. Tikudziwa mosakayika kuti Adamu ndi Heva anali anthu eni eni monga tidziwira bambo ndi mayi lero, koma tionanso kuti njoka yoyambayo idali ndi nzeru zimene zidaposa nzeru za njoka ya lero moterodi, njoka ya lero siyilankhula monga yoyambayo inkachitira.
2. Mfundo zotsatirazi, zikutitsimikizira kuti mitu yoyamba ya m’Buku la Genesis iyenera kuwerengedwa ngati mmene inalembedwera osayikapo kapena kuchotsera ndipo kuti nkofunika kukhulupirira izi kuti ndi zoonza ndithu:-

- Yesu anatsimikiza kuti chiphunzitso chake chofotokozera za ukwati chagona kwambiri pa chilengedwe cha Adamu ndi Heva ngati banja loyambirira la chitsanzo pamene ananenapo ngati nkoyenera kwa akhristu kusiyana pa ukwati kapena ayi (Mateyu 19:5-6); Palibe umboni wina umene tingaupeze m’Baibulo umene umanena kuti Yesu adawerengapo izi moyerekeza ayi.

- Ife sitikuonapo umboni ulionse woonetsa kuti malembo onena za chilengedwe m’Buku la Genesis aziwerengedwa mophiphiritsa. Timawerenga kuti dziko lonseli lidalengedwa mmasiku asanu ndi limodzi m’Buku la Genesis 1. Kutu awa adali masiku eni eni sinkhambakamwa chabe ayi; ndipo titsimikizira zonsezi poonanso kuti mwa zinthu zosiyana siyana padziko, chinthu chirichonse chidalengedwa patsiku losiyananso ndi gulu la zinthu zina ngakhale kuti zonsezo zimatsamirana pakufunika kwake. Timamvanso kuti ngakhale Adamu adalengedwa tsiku la chisanu nchimodzi, iye anafa patatha zaka mazana asanu ndi anai, kudzanso makumi atatu.

- Tikumvanso tikawerenga pa Eksodo 20:10,11 kuti tsiku la Sabata liri ndi maola makuni awiri ndi mphambu zinai zoyenera

kumapuma, chifukwa Mulungu anapuma patsiku la chisanu ndi chiwiri atagwira ntchito kwa masiku asanu ndi limodzi (ndipo momwemo, Israeli anasunga tsiku la Sabata poyambapo).

3. Chifukwa chakuti njokayo inapatsidwa chilango choti izikwawa ndi pamimba pake (Genesis 3:14), ife tikuganiza kuti njokayo idali ndi miyendo poyamba komanso kuphatikiza apo, idali ndi mphamvu yoganiza payokha. Njoka yoyambayo kotero, iyenera kuti idali ndi umoyo ofananapo ndi wa munthu. Ngakhale idali imodzi mwa nyama zonse zimene Mulungu analenga (Genesis 3:1 ndi 14), iyo inayandikirabe pofanana ndi munthu mchilankhulo.
4. Mwina nkutheka, njoka ija inali italawa kale chipatso chija cha mtengo wozindikiritsa kotero, nchifukwa chake idaoneka yochenjeretsa. Heva ***“anaona....kuti mtengo unali wabwino kudya, ndikuti unali wokoma m’maso, mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru,”*** (Genesis 3:6). Heva akanadziwa bwanji izi ngati iye sanaone chotsatira pakudya chipatsocho mu umoyo wa chinthu chimene chinadya kale ? Tionanso kuti Heva ndi njokayo anali akulankhulana kawiri kawiri pamwamba pa kulankhulana kumene kwalembedwa mu Genesis 3. Onani kuti liwu lolembedwa loyamba lolankhula njoka kwa mkaziyo likuonetseratu kuti nkhanayi inali itakambidwapo kale nthawi ina ndipo apa kunali kupitiriza zokambirana zimene zinayambidwa kalezo.

MPATUKO 19: LUSIFALA

“Wagwadi kuchokera kumwamba, iwe nthanda mwana wa mbandakucha! Wagwetsedwa pansu, iwe wolefuka amitundu! Ndipo iwe unati muntima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; Ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m’malekezero a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wammwambamwamba...”

MMENE ANTHU AMBIRI AMANENERA

Akhristu ena amanena kuti ati Lusifala adali mngelo amene sanamvera Mulungu mnthawi ya Adamu ndipo kuti adaponyedwa padziko lapansi, kumene iye Lusifala akuyambitsa mabvuto osiyana siyana pakati pa anthu. Mwaichi, anthu tsopano akuchimwa pamaso pa Yehova chifukwa cha Satana.

NDEMANGA:

1. Onani kuti mau oti ‘*mdierekezi*’ ‘*Satana*’ ndi ‘*mngelo*’ sadalembedwe pa ndime zimenezi komanso mmutu wonse wa Buku limeneli. Ndipo kuti ndi ndime yokhayi m’Baibulo imene yalemba za liwu kapena tinene kuti za dzina loti “*Lusifala*”.
2. Palibe umboni wotsimikizira kuti Buku la Yesaya 14 likukamba za zimene zidachitika mmunda wa Edeni; Ngati izi ziri choncho, chifukwa chiyani nkhanayi yalembedwa patatha zaka 3,000 popeza Buku la Genesis lidali litalembedwa kale pamene Yesaya ankalemba Buku lakelo?
3. Lusifalayu tikuwerenganso kuti anakwiriridwa ndi nyongolotsi (vs.11) ndipo kuti ananyozedwa, nasekedwa ndi anthu amene iye wakhala akuwazunza (vs.16) chifukwa chakuti apa tsopano alibiretu mphamvu zimene adali nazo poyambapo asanaponyedwe padziko lapansi lino kuchoka kumwamba (vs.5-8); (kapena ife timasulire kuti ‘asanalandidwe mphamvu za ulamuliro wa dziko lapansi zimene anali nazo poyamba) Choncho, nkobvuta kutsimikizira kuti lero Lusifala akadalipo ndipo akutsogolera anthu kumachimo padziko lapansi. Tonse timadziwa kuti machimo amabwera chifukwa cha zilako lako zathu zochokera mmitima yathu (Yakobo 1:14).
4. Chifukwa chiyani Lusifala akulangidwa mndime imeneyi pamene ananena kuti “*Ndidzakwera pamwamba pa mitambo*” (vs.13) ngati ife timakhulupirira kwathunthu kuti panthawi yoyambayo Lusifalayo anali kale kumwamba kalelo?
5. Tikuwerenganso kuti Lusifala adzaola m’manda: “*Chifumu chako chatsitsidwa kungsi ku manda, mbozi zayalidwa pansu iwe, ndi nyongolotsi zakukuta iwe*” (vs.11). Ndipo tikuwerenga kuti angelo samafa (Luka 20:35-36), Lusifala kotero, sanali mngelo chifukwa tamva kale kuti thupi lake linaola! Zonse zimene zinalembedwa apa choncho, zikukamba za munthu wapadziko amene akachimwa, amafa naola.

6. Ndime 13 ndi 14 zikugwirizana kwathunthu ndi Buku la 2 Atesalonika 2:3-4 pamene tikuwerengapo za *munthu wochimwa*. Nkoyenera choncho, kunena kuti nkhani ya Lusifala ikufotokoza za munthu osati mngelo wakumwamba monga timamvera kwa ena ayi.

ZIMENE NDIMEYI IKUNENA:

1. Ma Babulo ambiri akufotokozera momveka bwino kuti mitu 13 mpaka 23 ya Buku la Yesaya likunena za kubvuta kwa atsogoleri a mayiko ena monga Babulo, Tyre, Aigupto ndi ena a mphamvu amene adabvutitsadi panthawiyo. Yesaya 14:4 akutiwunikira izi potipatsa chithunzi thunzi kuti tiganizire: “*...pamenepo udzayimbira mfumu yaku Babulo nyimbo iyi yantchichi...*” Uneneri uwu motero, udali wa mfumu ya Babulo imene liwu lake lamasuliridwa kuti ndi “Lusifala” pa nunsu imeneyi. Tsiku limene mfumuyi idzagwe kotero, “*Two amene akuona iwe adzayang’anitsitsa iwe, nadzalingalira za iwe ndikuti ‘kodi uyu ndi munthu amene ananthunthumiritsa dziko lapansi...?’*” (vs.16). Mwaichi, tioneratu kuti ‘Lusifala’ ameneyu ndi munthudi!
2. Chifukwa chakuti ‘Lusifala’ anali munthu, mfumu ya ku Babulo, “*...ngakhale onse akulu akulu a dziko lapansi; kukweza kuchokera m’ mipando yawo mafumu onse a mitundu, onse adzabvomereza, nadzati kwa iwe, kodi iwe wakhalanso wopanda mphamvu ngati ife? Kodi iwe wafanana nafe?*” (vs.9-10). Lusifala momwemodi adali mfumu wamba monga mafumu ena onse padziko wokhala ndi mphamvu, kenaka nakhalanso wopanda mphamvu.
3. Ndime ya 20 ikunena kuti mbeu ya Lusifala idzaphwanyidwa nionongedwa. Tikawerenga ndime 22, tiona kuti ikunena kuti mbeu ya Babulo idzaonongedwa; apa ndiye kuti mbeu ya ndime imeneyi ikufanana ndi mbeu yoyamba ija ya mu ndime 20 imene ndi mbeu ya Lusifala kotero, zonsezi ndizo mbeu imodzi yomweyo. Mbeu yosamvera ndiyo mbeu yatchimo, chotsatira chake ndi imfa.
4. Kumbukirani kuti iyi idali “*ntchichi*” chabe, “*chiphiphiritso pa mfumu ya Babulo*” (vs.4). Mau oti ‘Lusifala’ ananthauzidwa kuti “*nthanda ya mbandakucha*” imene ili nyenyezi yowala kwambiri kuposa nyenyezi zina zonse. Mnkhanayi, nyenyeziyi inaganiza (onani kuti nyenyezi siyiganiza) zodzikweza pamwamba “*..ndidzakwera*

kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu” (vs.13). Chifukwa chaichi, nyenyeziyo inaponyedwa padziko lapansi. Nyenyeziyi ikuyimira mfumu ya Babulo imene mphamvu zake zinathetsedwa.

Danieli 4 akunena mwatchutchutchu za mmene mfumu Nebukadnezara mfumu ya Babulo inadzikuzira nidzitamandira pa ufumu wake umene inakhazikitsa, niiganiza kuti idagonjetsa ma ufumu ena ndi mphamvu zake osati zochokera kwa Yehova. *“...pakuti ukulu wanu wakula, nufikira kumwamba..,* (vs.22). Chifukwa chaichi, *“...anamuinga kumchotsa kwa anthu; nadya udzu ngati ng’ombe iye, ndithupi lake linakhathamira mame akumwamba, mpaka tsitsi lake lidamera ngati nthenga za chiombankhanga ndi makadabo ake ngati makadabo a mbalame*” (vs.33). Kugwetsedwa kumeneku ndiko kuponyedwa pansi kwa *“nyenyezi ya m’mbandakucha”* ija kuchokera kumwamba. Nyenyezi zimayimira udindo kapena ufumu m’Baibulo mwachitsanzo, Genesis 37:9; Yesaya 13:10 (ponena za atsogoleri a Babulo); Ezekieli 32:7 (ponena za mdindo wa Aigupto); Danieli 8:10 cp. vs.24. Kukwera kumwamba ndiko kutanthauza kudzikuzi ndipo kuponyedwa pansi ndiko kutsitsidwa pa udindo kapena kuchotsedwa pa ufumu – onani Yobu 20:6; Yeremiya 51:53 (za Babulo); Maliro 2:1; Mateyu 11:23 (kunena za Kaperna): *“Ndipo iwe, Kaperna, udzakwezedwa kodi kufikira kuthambo? Udzatsitsidwa kodi kufikira kumanda?”* Amene amatsikira kumanda ndi munthu.

5. Ndime 17 ikudzudzula Lusifala poononga dziko lapansi kukhala ‘chipululu’ *“...amene anapululutsa dziko, napasula midzi yake, amene sanamasula ndende zake zinke kwao?” ...ndi kudzaza dziko lapansi ndi midzi”.... “woyesedwa ndi mlingo wa golide”* (vs.17,21; vs.4). Izi zonse ndizo malongosoledwe a zochita za asirikali aku Babulo, kuononga malo onse okwera kuti akhale chigwa (monga anachitira ku Yerusalemu), kugwira ukapolo anthu ndikuwasamutsira kumalo achilendo amene anthuwo sakuwadziwa ndipo osawabwezeretsa kwao (monga anachita kwa a Yuda), namanga midzi yawo kwa eniwo, nawalanda miyala ya mtengo wapatali kuti iwo adzilemeletse mwa iwo wokha eniwo akusauka. Nchifukwa chake Lusifala, anenedwa kuti sadzayikidwa mmanda mwaulemerero

- monga ena anayikidwa ayi, izi zidzakhala choncho, chifukwa chofuna kumulanga pa zoyipa zomwe iye anachitira anthu enawo (vs.18-19); kutsimikiziradi kuti iye anali munthu osati mngelo ayi.
6. Ndime 12 ikunena kuti Lusifala **“wagwetsedwa pansu,”** ngati mtengo wachiyimire. Ndimeyi ikugwirizana ndi ndime ya Danieli 4:8-16, pamene mfumu Nebukadnezara ndi Babulo afananizidwa ndi mtengo wogwetsedwawo.
 7. Babulo ndi Assuri akufotokozedwa ngati liwu lotanthauza chinthu chimodzimidzi mmabuku a Aneneri; ndipo polankhula zaizi, kugwetsedwa kwa mfumu ya Babulo mndime ya 25 akuti; **“...ndidzathyola Assuri...”**. Ulosi wa Babulo pa Yesaya 47 ukubwerezedwa ponenanso za Assuri pa Nahumu 3:4,5,18 komanso pa Zefaniya 2:13,15; ndi 2 Mbiri 33:11 pamene tikuwerenga kuti mfumu ya Assuri inagwira ukapolo mfuko la Manase napita nalo ku Babulo. Amosi 5:27 akunena kuti Israeli anayenera kupita ku ukapolo *‘modutsa ku Damasiko’* kutanthauza kuti kunali ku Assuri, koma Stefano akunena kuti uku kunayeneradi kukhala kuyenda *‘mopitirira ku Babulo’* (Machitidwe 7:43). Ezra 6:1 akufotokoza za Dariusi mfumu ya Babulo imene idalamula kuti kachisi wa Chiuta akonzedwenso. A Yuda anayamika Mulungu wao pofewetsa mtima **“wa mfumu ya Assuri”** (Ezra 6:22) ndipo izi tiona kuti zikufanana. Uneneri wa Yesaya 14, ndi uneneri wina m’Buku lomweli, ukugwirizana kwathunthu ndi zimene mfumu Sennakeribu anachita pamene mfumu Hezekiya ankalamulira, koteronso, ndime 2 ikufotokozerana za kudulidwa kwa ufumu wa Assuri. Ndime 13 ikumveka mosabvutikira kuzindikira za mnyozo umene Assuri anachita polowa mu mzinda wa Yerusalemu, nalanda kachisi wa Yehova, ndikuikamo milungu yawo. Koyambirira, mfumu ya Assuri Tigileti Pilese ankafuna kuchita chimodzi modzi (2 Mbiri 28:20,21); Yesaya 14:13: **“Ndipo unati mu mtima mwako, Ndidzakwera kumwamba,”** (kuyimira Kachisi ndi Gome la Guwa – 1 Mafumu 8:30; 2 Mbiri 30:27; Masalmo 20:2,6; 11:4; A Hebri 7:26). **“Ndipo ndidzakhalanso pamwamba pa phiri la Zioni...”** (kumene Kachisi adamangidwa – Yerusalemu ; Masalmo 48:1,2).

MPATUKO 20: MAYESERO A YESU

Mateyu 4:1-11; *“Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kuchipululu kukayesedwa ndi Mdierekezi..... pomwepo Mdierekezi anamsiya Iye, ndipo onani, m’ngelo anadza, namtumikira Iye”*

MMENE ANTHU AMBIRI AMAMVERA:

Anthu ambiri akawerenga ndime imeneyi, amanena kuti ikutanthauza kuti chinthu china chotchchedwa Mdierekezi chinamuyesa Yesu, chimupangira zoti achite pomunyengerera Iye kuti achimwe ali ku chipululuko.

NDEMANGA:

1. Yesu *“anayesedwa mnjira zonse monga ife timayesedwa mosiyana siyana lero lino”* (A Hebri 4:15), koma *“...munthu aliyense ayesedwa pamene chilako lako chake cha iye mwini chimkokera, nichimnyenga”* (Yakobo 1:14). Ife timayesedwa ndi *“mdierekezi”* amene ali *‘zofuna ndi zilako lako zathu’* zoganiza zoyipa mmitima mwathu, ndipo Yesu anayesedwanso chimodzimidzi. Motero, ife sityesedwa ndi chinthu china choyenda pachokha monga ena amalalikira ayi. Tchimo ndi mayesero zonse zimadza chifukwa cha zolaka laka za muntima mwathu (Marko 7:21).
2. Mayesero aja a Yesu sayenera kuwerengedwa monga adalembedwa chifukwa:-
 - Mateyu 4:8 timawuzidwa kuti Yesu anatsogozedwa ku phiri lalitali kuti akaone maufumu onse a dziko lonse *“mkamphindi”* (Mateyu 4:5). Tikaganiza bwino, tiona kuti palibe phiri lalitali mdziko lapansi limene titakwerapo lingatipangitse kuti tione maufumu onse padziko. Komanso tikawerenga ma Baibulo omasuliridwa bwino, akuti pokwera paphirilo, Yesu anaonetsedwa maufumu ngati momwe adzakhalire kutsogoloko osati panthawi imene Yesu ankayesedwayo ayi. Apa ndipamene ife tikunenera kuti Yesu anawonetsedwa maufumu a nthawi ino ndinso ena amene akubwerabe Khristuyo asanabwerenso padziko lapansi lino.
 - Mukawerenga Mateyu 4 kenaka nkuwerenganso Luka 4, muona kuti pali kusiyana pa kalembedwe ka nkhani imeneyi.

Ndondomeko yake ikusiyani. Marko 1:13 akunena kuti Yesu *“anakhala mchipululu masiku makumi anai oyeseledwa ndi Satana”* pamene Mateyu 4:2-3 akuti *“Ndipo pamene Iye analibe kudya (anasala) masiku makumi anai usana ndi usiku... woyesayo anafika nanena kwa Iye...”* Popeza Mau a Mulungu samadzitsutsa, tikuona kuti mayeserowa ayenera kuti ankabwerezedwa bwerezedwa. Yesero losandutsa miyala kukhala mikate ndicho chitsanzo choonekeratu pa nkhani imeneyi. Koteru, anali mayesero amene Yesu ankamubwerera kawiri kawiri mmaganizo mwake osati zinthu zeni zeni zimene zinkachitika ayi. Tikunena izi popeza taona kuti Iye anali mu uthunthu ndi umunthu ngati wathu. Iye koteru, adayamba kumangoganizira chabe zinthuzi popeza sizikanatheka kuti achite zozizwitsa chifukwa nthawi yake inali isanafike. Timadziwa tonse zimene zimachitika munthu akakhala osadya kwa masiku angapo kuti amafunitsitsa chakudya chifukwa cholakalaka atadya kanthu kenaka atha kuyamba zirubwe rubwe chifukwa cha njala (1 Samueli 30:12). Zifani fani za miyala ndi mkate zikambidwanso ndi Yesu m’Buku la Mateyu 7:9, ndipo izi zikutionetseratu mmene Yesu anamvera mthupi mwake pamene ankayeseledwa mntthawi imene Iye ankasalayo.

- Zikhoza kutheka kuti Yesu anangowauza akuphunzira ake aja za mayesero ake amene Iye anabvutika nawo koyambirira kwa moyo wake wapadziko lino. Zitha kuthekanso kuti ankafotokoza nkhanayi mophiphiritsa kwa akuphunzira akewo pofuna kuonetsa mmene anazunikira muntima mwake ngati mmene tikuonera pa Mateyu mutu wa 4 ndi Luka 4.
- Zikuonekanso kuti pamene Yesu akuti anatengedwa mmisewu ya mu Mzinda wa Yerusalemu, nakwezedwa pamwamba pa Kachisi kuti awone dziko lonse, a Yuda sanathe kumuona panthawiyo. Tikawerenga mabuku a mbiri yakale monga amene analembedwa ndi Josephusi, izi sizinalembedwe pena paliponse ngati momwe timawerengera malo ena choncho, sizingakhale kuti zinachitikadi monga ena amaganizira ayi. Phiri lalitali kwambiri ku Israeli likhoza kupezeka ku mapiri a ‘Hermon’ ndipo phirilo lili kutali kwambiri ndi Yerusalemu. Komanso sizikanatheka kuti Yesu ayende mmasiku amenewa kuchokera ku Hermon nkukafika ku

Yerusalemu pokha pokha ngati anali mayesero mmaganizo mwake mwa Yesu. Komanso, tamva kuti mayesero ake onse a Yesu anachitikira mchipululu (nayesedwa ndi Satana amene anachoka komaliza kwamayesero – Mateyu 4:11). Koteronso, oyesayo anayesa tsiku ndi tsiku osachoka mpaka tsiku lomalizalo. Mwaichi, tikhoza kuona kuti izi zonse zinkachitika mmaganizo a Yesu nchifukwa chake, akuoneka kuti ankayendayenda mmalo otalikirana mosabvuta popeza anali mmaganizo chabe. Ndipo izi zigwirizanadi ndi Yakobo 1:14 kuti ife timachimwa ndi kuyesedwa mmaganizo, zilako lako ndi zofuna za thupi lathu.

- Ngati mdierekezi ndi chinthu choyenda chimene chimachimwitsa anthu, kukanakhala kobvuta kuti chinthu chosamvachi, chichoke ndi mau a Mulungu. Onani kuti Yesu akusanthula Mau a Mulungu nthawi zonse mwachitsanzo, maganizo oyipa akutsutsana ndi maganizo ochokera m’Buku Loyera. Izi zikumveka bwino kuti Yesu nthawi zonse akutiphunzitsa kukumbukira Mau a Mulungu pamene tiyesedwa ndi maganizo oyipa mmitima mwathu. Masalmo 119:11 akutitsimikizira bwino izi pamene timawerenga za ulosi onena za mayesero ndi mabvuto a Yesu Khristu mchipululu: “*..Ndinawabisa Mau anu mumtima mwanga kuti ndisachimwire Inu*”.
- Mateyu 4:1 akunena kuti “*...Pemenepo Yesu anatsogozedwa ndi Mzimu kumka kuchipululu kukayesedwa ndi mdierekezi*” uwu udali Mzimu wa Mulungu umene Iye anadzozedwa nawo (mutu 3:16). Sizingakhale zoyenera kuti Mzimu wa Mulungu ungumulondolere kuchipululu kuti Yesu akayesedwe ndi chinthu chimene chitsutsana ndi Mulungu wamphamvu amenenso ali wodziwa kuyesa.

ZIMENE NDIMEYI IKUNENA

1. Pamene Yesu anabatizidwa mu mtsinje wa Yordano mu ubatizo wa Yohane, atangobatizidwa, analandira mphamvu ya Mzimu Woyera (Mateyu 3:16). Atangotumphuka kuchokera mmadzi, anatsogozedwa ndi kumka kukayesedwa. Pozindikira kuti anali ndi mphamvu ya Mzimu, anafunsidwa kuti angosandutsa miyala kukhala mkate, kudumpha kuchokera pamwamba pa denga la kachisi koma osabvulala popeza angelo akanamuwakha ndi zina zotero. Mayesero

amenewa tiona kuti ndi amene anabvutitsa koposa mmaganizo mwake. Tikuona kuti nkwapafupi kwa munthu (Yesu mnjira imeneyi) kuyesedwa mmaganizo ake kusiyana ndi kuti wina wapadera achite kukuyesa monga tikuwerengera pa Yakobo 1:14.

2. Mayesero olamulira maufumu akhozanso kufika kolimba mmaganizo a munthu kusiyana ndi kuti munthuyo awuzidwe kuti aganize monga wina akuganizira kayesedwe. Yesu anali ozindikira kwambiri Mau a Mulungu panthawiyo ndipo chifukwa cha mazunzowa, komanso kusala kumene Iye anachita, sichinali chapatali kuti ayambe kumasulira Mauwo mogwirizana ndi mmene Iye analakalaka kuti zinthu zikhaliire muntima mwake. Kuyima pamwamba kukutikumbutsa Ezeieli pamene awonetsa kuti kuchokera pamwamba paphiri, ufumu uwoneka ngati wochokera pamwamba paphirilo (Ezeieli 40:2), ndinso Yohane amene anaona; **“...mzinda wopatulikawo, Yerusalemu wochokera pamwambamwamba paphiri”** (Chibvu. 21:10). Yesu anaona maufumu a dziko lonse lapansi mmene akanakhala kutsogolo kwake (Luka 4:5), mwachitsanzo, muufumu wa kumwamba pamene **“maufumu a dziko lapansi ayamba kukhala a Ambuye wathu, ndi wa Khristu Yesu..”** (Chibvu. 11:15). Mwina Yesu apa anaganizira za Mose pomaliza kwa zaka makumi anai mchipululu akuyendayenda. Masiku makumi anai ake ali mchipululu, anakhala akuyang’ana dziko la malonjezano (ufumu) kuchokera m’phiri la Nebo. Ndipo zitsimikizidwa izi powerenga (Danieli 4:17, 25,32; 5:21) kuti **“...Wamwambamwamba alamulira m’ufumu wa anthu, naupereka kwa aliyense Iye afuna...”** Yesu anayenera kudziwa kuti ndi Mulungu yekha amene akanamupatsa ufumuwo. Choncho, tione kuti siyesero lolimba kwa Iye ngati chinthu china chitamuyesa kuti akhulupirire zosiyana ndi zimene Yesuyo ankazidziwa kale. Nchifukwa chake, tikutha kuona kuti mayeserowa ayeneradi kuchokera mmaganizo ake kuti tsopano atha kutengeratu ufumuwo asanagwire ntchito yake. Mwachitsanzo, anatha kuganiza kuti wapatsidwa mphamvu zonse ndi ulamuliro wonse kuti ayembekezere kukhala mfumu (Luka 5:26,27), mpaka kuti athanso kupereka mphamvu, moyo ndi ulamuliro komanso kuzilanda zonsezi (Yohane 10:18), ngakhale kuti mphamvu zonse zinapatsidwadi kwa Iye pamene anafa naukanso (Mateyu 28:18).

3. Chifukwa chakuti anadziwa kwambiri Mau a Yehova, Khristu anatha kuona kufanana kwake pakati pa Iye ndi Eliya, amene patatha masiku makumi anai, nyonga zake pachikhulupiro chake zinayamba kumwazika mchipululu chija (1 Mafumu 19:8) ndipo Mose, analepheranso kukafika mdziko lamalonjezano pomaliza kwa zaka makumi anai mchipululu. Pomaliza masiku makumi anai, Yesu anafanana ndipo kuti anatsala pang'ono kulephera ngati momwe Mose ndi Eliya analepherera chifukwa cha umunthu wao ofooka osati chifukwa cha mdierekezi ayi. Momwemonso, Yesu anafooka mu umunthu wake omwewo, chifukwa chake, '*satana*' kapena tinene kuti '*mdierekezi*' ameneyu mumtima mwake ndi amene anamuyesa Yesu. Mwanjira ina tinene kuti anadziyesa (Iye ngati mdierekezi) pa Iye yekha.
4. "*Ndipo mdierekezi anati kwa Iye, Ngati muli Mwana wa Mulungu, uzani mwala uwu usanduke mkate*" (Luka 4:3). Udali mtsutso waukulu mumtima mwa Yesu ndipo mopitiriza ankadzifunsa ngati adalidi Mwana wa Mulungu, poona kuti anthu onse ankaganiza kuti Iye anali Mwana wa Yosefe (Luka 3:23; Yohane 6:42) komanso kuti ankamuona ngati mwana wa mtchire popeza analibe bambo wake (Yohane 9:29) popitiriza apa kalemba wa mkachisi anamutchula Iye ngati mwana wa Yosefe (Mateyu 1:1,16; Luka 3:23). Iye ndiyekhayo munthu amene anakhala padziko lapansi mwana wopanda bambo . A Filipi 2:8 akutsimikizira kuti Khristu anakhulupirira nabvomereza kuti Iye analidi munthu ngati ife, kutanthauza kuti kunali kotheka kwa Iye kuti asadzikhulupirire koma kudzikayikira kuti Iye anali Mwana wa Mulungu, kenakanso nadzikayikira pa umunthu wake.
5. Tadziwa kuti mayesero a Yesu aja anatsogoleredwa ndi Mulungu ndipo chinali cholinga cha Yehova kuti Khristu aphunzire za chipiriro mu uzimu. Ndime zimene Yesu anakumbutsa anthu za kwaipa komanso udierekezi zinkanena za mau olembedwa mu Buku la Deuteronomo limene limafotokoza za mbiri ya Israeli ndi zobvuta zawo pamene anali mchipululu muja. Yesu choncho, anaona kufanana pakati pa mbiri imeneyi ndi zomwe Iye ankaona pamoyo wake panthawiyo.

DEUTERONOMO 8.

Vs.2 *“...Yehova Mulungu wanu anakuyendetsani mchipululu zaka izi makumi anai, kuti akuchepetseni, kudziwa chokhala mumtima mwanu, ngati mudzasunga malamulo ake, kapena iai..”*

Vs. 3 *“Ndipo anakuchepetsani (Mulungu), nakumvetsani njala, nakudyetsani ndi mana, ..kuti akudziwitseni kuti munthu sakhala wamoyo ndi mkate wokha koma munthu akhala wamoyo ndi zonse zotuluka mkamwa mwa Yehova”*

“Ndipo muzindikire mmtima mwanu, kuti monga munthu alanga mwana wake, momwemo Yehova Mulungu wanu akulangani inu.

MATEYU 4 / LUKA 4

“Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kuchipululu masiku makumi anai.” Yesu anakwaniritsa mayesero. Yesu anagonjetsa mayeserowo pokumbukira Mau Oyera mumtima mwake (Masalmo 119:11).

“...anamva njala...” Pa Yohane 6, mana akumasuliridwa ndi Yesu ngati liwu loyimira ‘Mau a Mulungu’ mtanthauzo lake. Yesu anaphunzira izi ndipo kuti anakhala ndi Mau a Mulungu. *“..Ndipo Yesu anayankha nati kwa iye, Kwalembedwa kuti munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mau ...a Mulungu.”* Mosakayikira, Yesu anakumbukira pamene anakumana ndi mabvuto amenewa. Mulungu kotero, analanga Mwana wake Yesu – 2 Samueli 7:14; Masalmo 89:32.

Motero, Yesu anationetsa mmene tiyenera kumvetsera Mau a Mulungu komanso kuwasunga mumtima mwathu. Iye anadziganizira ngati mmene ana a Israeli mchipululu analiri ndipo potero, anaphunzirapo kanthu pamene Iye analinso mchipululu.

MPATUKO 21: NKHONDO MMWAMBA

“Ndipo munali nkhondo mmwamba. Mikayeli ndi angelo ake akuchita nkhondo ndi chinjoka; Chinjokanso ndi angelo ake chinachita nkhondo; ndipo sichinalakika ndipo sanapezekanso malo awo mmwamba. Ndipo chinaponyedwa pansu chinjoka chachikulu, njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wadziko lonse;

chinaponyedwa pansi padziko , ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi.....”

MMENE ANTHU AMBIRI AMAMVERA:

Iyi ndi ndime imodzi imene anthu ambiri amaona kuti imawatsimikizira mfundo yoti kunali mkangano kumwamba pakati pa angelo ndiponso kuti ichi, chinapangitsa kuti mdierekezi ndi angelo ake onse aponyedwe padziko lapansi, kumene mu uthunthu wa njoka, anayambitsa mabvuto ndi tchimo pakati pa anthu.

NDEMANGA:

1. Taphunzira zinthu zambiri tsopano zimene ziyenera kutithandiza pa chizindikiritso cha nkhani imeneyi. Taona kuti angelo samachimwa kotero, sizingatheke kuti kumwamba kungakhale mkangano wina uliwonse chifukwa mkangano ndiwo tchimo. Kotero, sikoyenera kumasulira ndime imeneyi kuti ionetse kuti angelo amachimwa kapenanso kuti angelowo anachimwa kale. Moteronso, angelo sangachimwitse anthu mwanjira iriyonse. Poonanso kuti tchimo limadza ndi kuyamba pamene munthu alakalaka mumtima mwake kuchita chinthu osati kuchokera kwa chinthu china chakutali monga ena amanenera ayi (Marko 7:20-23).
2. Njoka ija (ya ndime ili pamwambayi) inaponyedwa pansi kuchokera kumwamba, kunena kuti poyamba inali kumwambako. Koma njoka yeni yeni yoyamba ija mu Edeni, inalengedwa ndi Mulungu kuchokera ku mfumbi (Gen.1:24-25). Choncho apa, sizikutanthauza kuti mdierekezi anachokera kumwamba naponyedwa pansi pano, kenaka nakalowa mwanjoka kuti izitichimwitsa ayi.
3. Onaninsu mwapadera kuti palibe pena paliponse apa pamene tingawerengepo zonena kuti angelo anachimwa komanso kuti amachimwa pamaso pa Mulungu. Mwaichi, palibe mngelo amene anamenya nkhondo ndi Mulungu mmwamba: “*...palibe wonditsutsa Ine...*” (Deuteronomo 32:39).
4. Tikawerenga mavesi 7-9, kenaka timamva pa ndime 10 kuti “*ndipo ndinamva mau akulu m’Mwamba, nanena, Tsopano zafika chipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu za Mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Khristu wake; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku*”. Ngati zimene tawerenga pa ndime 7-9 zinali zoyambirira kuchitika

poyamba kwa dziko lonse Adamu ndi Heva asanalengedwe, zitheka bwanji kuti chipulumutso cha munthu chiyambe panthawiyi? Adamu atachimwa, munthu anayamba kupezana ndi mabvuto ngati tchimo, njala, ukapolo ndinso kulephera zomwe sizingatchulidwe **“chipulumutso ndi ufumu wa Mulungu”**. mdierekezi ataponyedwa pansi pano mindime imeneyi, tikumva kuti kunali kusangalala chifukwa chakuponyedwako. Chifukwa chiyani kunali kusangalala ngati kubwera kwake kunayenera kubweretsa tchimo, imfa, ukapolo ndi mabvuto ena pakati pa anthu? Ngati kugwetsedwa kuchokera kumwamba kugwa pansi pano timva mwachiphiphiritso, monga kutanthauzira kugwetsedwa pa udindo (werengani Yesaya 14:12; Yereimiya 51:53; Maliro 2:1; Mateyu 11:23), tiona kuti tikhala ndi chithunzi thunzi chabwino pankhani zonzezi. Ndipo izi zikhala kuti zinachitika Adamu asanalengedwe choncho, asanachimwe, zitheka bwanji kuti mdierekezi anyoze anthu poona kuti anthuwo anali asanalengedwe?

5. Tiyenera tidziwe kuti palibe chikuonetsa kuti zinthu izi zinachitikira mmunda wa Edeni. Mfundo yofunika yalembedwa pa Chibvumbulutso 1:1 ndi 4:1 – kuti Buku la Chibvumbulutso ndilo **“Chibvumbulutso cha Ambuye wathu Yesu Khristu...cha izi ziyenera kuchitika posachedwapa”**. Nkhaniyi choncho, sindiye kuti inachitika kale mmunda wa Edeni ayi koma ‘ziyenera kuchitika posachedwapa’ mchirumika choyamba Yesu atangokwera kumwamba. Chibvumbulutso chimenechi chinapatsidwa kwa Yohane ndi Yesu Khristu. Yense amene angawerenge izi awona kuti nkhanayi siyinachitike mmunda wa Edeni ayi koma zinayenera kuchitika kutsogoloko. Mwaichi, nkhanu ya mdierekezi mindime imeneyi sikugwirizana mpang’ono pomwe ndi zimene zinachitika mmunda wa Edeni.
6. **“Chinjoka chachikulu...njoka yokalambayo”** (Chibvu. 12:9). Njokayo inali ndi **“...mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi”** (vs.3), koteru, sikuti inalidi njoka yeni yeni. Ponena kuti **“...njoka yokalambayo..”** Zionetsa kuti idalidi ndi zochitika zofanana ndi njoka ya mmunda wa Edeni ija, monga ponyengerera ngati njoka yoyambayo. Moteronso, **“...mbola ya imfa ndiyo uchimo.”** (1 Akorinto 15:56). Koma sizitanthauza kuti imfayo ndiyo njoka ayi. Imfa ili ndi zofanana mwanjokayo popeza zonse zikhudzana ndi tchimo.
7. Mdierekezi anaponyedwa pansi padziko ndipo anali okakala mtima chifukwa **“...podziwa kuti katsalira kanthawi”** (vs.12). Tionanso kuti ngati Satana anaponyedwa padziko lapansi mu Edeni muja, ndiye kuti anayenera

kukhala ndi mpata waukulu osokoneza munthu ngakhale izi sizikugwirizana ndi mau oti *'kamphindi'*.

8. Kodi mdierekezi akananamiza bwanji dziko lapansi lonse asanaponyedwe padziko lapansilo (vs. 9) popeza padzikolo palibenso munthu wina aliyense chifukwa Adamu amene adali munthu woyamba padziko anali asanalengedwe panthawiyi.
9. Mndime 4, tiwerenga kuti chinjokacho chinanyamula mbali yachitatu ya nyenyezi zonse zakumwamba pogwiritsa ntchito mchira ndipo nyenyezizo zinaponyedwa pansu pano pamodzi ndi chinjokacho. Ngati tiwerenga izi mosaphiphiritsa, ndiye kuti Chibvumbulutso chonse cha Mutu 12 chiyenera kuwerengedwanso mosaphiphiritsa ndipo tiona kuti timvetse bwino monga za kukula kwake kwa chinjokacho – kupitirira mbali ya chitatu ya dziko lonse, ikufanana ndi mchira wake wokha! Apa ndiye kuti dziko lapansi lacheperatu. Tikudziwanso kuti nyenyezi zambiri ndi zazikulu kuposa dziko lathu lino lapansi choncho, zitheka bwanji kuti mbali ya chitatu ya nyenyezi zonse zitere padziko lapansi lomwe ndi laling'ono kuposa nyenyezi ngakhale imodzi yokha. Mwachitsanzo, nyenyezi imodzi ndi yaitali komanso yokwanira ma 'kilomita' oposa 15 'trillion'. Uku tinganene kuti ndiko kotalika kwa mchira wa njokayo, nanga thunthu lakelo lingakhale bwanji? Tinene kotero, kuti nkhanayi ndichiphiphiritso chabe.
10. Monga takambirana pa zimene zidalembedwa m'Buku la Chibvumbulutso 12 ndi uneneri wake, nzosadabwitsa kuwerenga pa Chibvumbulutso 1:1 kuti nkhanayi inalembedwa mchiphiphiritso popereka zizindikiro zimene ziyenera kumasuliridwa bwino. Tiona izi makamaka pamene tiwerenga Chibvumbulutso 12:1 pomwe liwu lofotokozerana za ntchito yotsatirayo latchedwa kuti ndicho *"chizindikiro chachikulu"*.
11. Powerenga za mdierekezi kuti akuchita chiyani pa dziko lapansi, sitikuona pena paliponse pamene palembedwa kuti mdierekezi amawachimwitsa anthu padziko ayi. Ndipo mmalo mwake, ndime 12-16 zikuonetsa kuti mdierekezi ndiwolephera kuchita chimenechi. Satana analephera kubweretsa mabvuto padziko lapansi chifukwa cha ntchito yopambana ya Yesu Khristu. Izi sizikugwirizana ndi zimene alaliki ambiri a lero amalalikira.
12. Mfunso limodzi lowonekeratu pa Chibvumbulutso 12 ngati uneneri wu unatsimikiziradi kuti kudali nkondo kumwambako ndilo; kodi liwu loti *'kumwamba'* lalembedwa mophiphiritsa ndi mwa chizindikiro kapena ayi.

Tinafotokozapo poyamba paja kuti liwu loti 'kumwamba' apa likhoza kuphiphiritsa udindo wa munthu. Nchifukwa chake Chibvumbulutso ngati Buku limodzi lolembedwa mzizindikiro motere, tipeza kuti mau'wa akukamba zinthu zonsezi mchiphiphiritso.

Mkazi amene tiwerenga pa ndime yoyamba (Vs.1) **"...wobvekedwa dzuwa, ndi mwezi kumapazi ake, ndi pamutu pake korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri;"** Zinthu zimenezi zomwe tawerenga kuti ndi za kumwamba, ndipo kuti zataidwa kuchoka kumwambako, siziyenera kuwerengedwa ngati mmene zalembedwera ayi. Mkaziyo mwachitsanzo, sizingatheke kuti abvekedwe dzuwa chifukwa tonse timadziwa kuti dzuwalo ndilalikulu komanso limaotcha kwambiri. Nyenyezi ndi zazikulu kwambirinsu kuposa dziko lapansi lino koteronso, sizingatheke kuti munthu abvekedwe ndi zinthu zimenezi pamutu pake. Chizindikiro china chimene chikuoneka mmwamba ndicho chimene chalembedwa pa vs.3 **"...chinjoka chofira"**. Nkhaniyi imatengedwa ngati yosaphiphiritsa yeniyeni koma siziyenera kukhala choncho. Mnkhanayi tiona pongowerenga chabe kuti ndichiphiphiritso cholembedwa pogwiritsa ntchito maina a zinthu ndi anthu ngati zizindikiro.

Ndime yachinai (vs.4) ikufotokozera za mmene chinjokacho chinakokera gawo lachitatu la nyenyezi za kumwamba nkuzigwetsera pansi pano. Taona kuti chifukwa chakukula kwa nyenyezi moyerekeza ndi dziko lapansi lino, sizingatheke kuti nkhanayi yakambidwa mosaphiphiritsa ayi. Ufumu wa Mulungu omwe ndi wa Kumwamba udzakhazikitsidwa pansi pano (Dan.2:44; Mateyu 5:5), zimene sizingakhale zotheka ngati dziko lino lidzaonongedwe ndi nyenyezi zomwe zidzagwere pansi pano chifukwa tikudziwa, nyenyezi imodzi yokha ndi yaikulu kuposa dziko lonse lapansi kotero, dziko lapansili likhoza kuphwasulidwa ngati patagwera nyenyezi ngakhale imodzi yokhayo.

Koyambirira kwa mutu umenewu, mkazi **"wammwamba"** (kenaka) anabala mwana wake wamwamuna, amene **"anakwatulidwa mwana wake amuke kwa Mulungu, ndi kumpano wachifumu wake"**. Malo a ufumu wa Mulungu ndiko kumwamba. Ngati mkaziyo anali kale kumwamba, sikungayenere kuti pokwatulidwa mwana wakeyo apitenso kumwamba komweko kumene mkaziyo aliko kale. Ichi kotero, ndicho chizindikiro chabe, chiphiphiritso cha nkhanayi poyerekeza nkhanayi ina ya dziko lapansi lino ngakhale kuti yakambidwa ngati nkhanayi ya kumwamba. Tikawerenga mopitiriza ndime zimenezi, tiona kuti

mkaziyu akuthawira ‘kuchipululu’. Tsono ngati izi zikuchitikiradi kumwamba kweni kweni, ndiye kuti kumwambako kulonso zipululu. Izi ife tikuona kuti sizingatheke ndipo tionanso kuti nzomveka bwino ngati kumwamba kumene kwakambidwa apaku kukuyimira chiphiphiritso cha malo ena koteru, chipulululo chikhoza kukhala chizindikiro chabe kapenanso ayi.

Tsopano tiyeni tione vs.7 – “...munali nkhondo mmwamba”. Ndime zonse zimene zikukamba za ‘kumwamba’ mchiphiphiritso m’Buku la Chibvumbulutso 12 zikutitsimikiziranso kuti nkhanu yonse ndi chizindikiro cha zinthu zimene zidzayenera kuchitika padziko lapansi kutsogolo kwa nkhanu imeneyi. Tanena motere chifukwa tsopano tikudziwa kuti kumwamba kweni kweniko kulibe kukangana (Mateyu 6:16; Masalmo 5:4,5; Habakuk 1:13). Chiphunzitso china chimanena za angelo ochimwa amene akuti amakhala mbali ina kumwambako yotchedwa Hade kapena kutinso ‘Hell’ amene ali malo achilango. Tikudziwa kuti mnkhaniyi, angelo ochimwa akunenedwawo, ali kumwamba choncho, kumwamba pano ndi chiphiphiritso cha malo ena koteronso, angelo pano alembedwanso mchiphiphiritso cha anthu ena.

Mfundo zimene alaliki ena amanena pa chiphunzitso cha mdierekezi ndi izi:

- (a) Mdierekezi adali mngelo wa Mulungu kumwamba koma anaponyedwa pansu pano mmunda wa Edeni chifukwa chosamvera ndi kuukira Mulungu. Anaponyedwa padziko lapansi mu Genesis 1.
- (b) Mdierekezi anayenera kubwera padziko lapansi nakwatira mu Genesis 6.
- (c) Munthawi ya Yobu, mdierekezi ankapezeka konse konse kumwamba ndi pansu pano.
- (d) Mnthawi ya Yesaya 14, anaponyedwa kuchokera kumwamba nagwera pansu pano.
- (e) Zekaliya 3, mdierekezi akupezekanso kumwamba.
- (f) Mateyu 4, mdierekezi ali padziko lapansi lino. “*watayidwa*” pamene Yesu anafa pamtanda paja.
- (g) Uneneri wina umapezeka tikawerenga Chibvumbulutso 12 onena kuti mdierekezi “*anaponyedwa*”.
- (h) Mdierekezi “*wamangidwa*” mu Chibvumbulutso 20 pamene mu Genesis tamva kuti Satana ndi angelo ake amangidwa kale makamaka tiwerenganso Yuda ndime yake ya 6. Ngati mdierekezi anamangidwa kale m’Chipangano Chakale, nchifukwa chiyani akumangidwanso mChipangano Chatsopano pa Chibvumbulutso 20?

Apa tiona kuti nkobvuta kunena kuti mdierekezi anamenya nkondo nakanidwa kumwamba, koma kuti zonse zolembedwa ponena za mdierekezi mndime zimenezi zinalembedwa mchiphiphiritso. Tikatero, tiona kuti nkhani yonse ikumveka bwino komanso moyenera.

ZIMENE NDIMEYI IKUNENA

1. Tikati tingomasulira ndime yokhayo pamene sitinamvetse kweni kweni Buku lonse la Chibvumbulutso, ndiye kuti tiphonya cholinga cheni cheni cha Uthenga Wabwino wa Bukuli.
2. Nkhondo imene ikukambidwa apayi ikuphiphiritisa pofotokozera zimene zidzachitike mzizindikiro za malo ndi maudindo a padziko lapansi pa kusiyana kwa zikhulupiro ndi zinthu zochita pakati pa anthu a Mulungu ndi anthu okonda za mdzikowo. Chiphiphiritsochi chinaneneratu za zinthu zimene ziyenera kuchitika kutsogolo kwa nthawi imeneyi. Onani kuti izi zinakambidwa pamene kunali mafumu okhazikitsidwa ndi maulamuliro a chi Yuda ndi chi Roma.
3. Kutu mdierekezi wanenedwa ngati chinjoka uja akuyimira udindo wa anthu ena mwa anthu a ndale, ukhoza kudziwika chifukwa **“wabwekedwa nduwira za ufumu zisanu ndi ziwiri”** pamutu pake (vs.3). Pa Chibvumbulutso 17:9,10 tionanso ndemanga imene yalembedwa za chinjokacho: **“Pano pali mtima wakukhala nayo nzeru”** ndiko kunena kuti osatenga chinjokacho ngati chinjoka cheni cheni ayi koma kuti; **“mitu isanu ndi iwiri ndiyo mapiri asanu ndi awiri...awa ali mafumu asanu ndi awiri.”** Mmodzi mwa mafumuwo akupitiriza **“kukhala kanthawi”** zomwe zikulumikizana ndi mdierekezi wa chinjokacho chimenenso **“kamtsarira kanthawi”** m’Chibvumbulutso 12:12.

PHUNZIRO 6: MAFUNSO

1. Kodi ndindani amene amayambitsa mabvuto ndi mayesero mwaife anthu?
(a) Mulungu (b) Zimangochitika (c) Chinthu chochimwa chotchedwa Satana (d) Zinthu zochimwa zotchedwa ma 'demoni'.
2. Ndindani amatitengera kumayesero kuti tizipezeka kuti tikuchimwa nthawi ndi nthawi?
(a) Uthunthu wathu wachilengedwe wauchimo (b) Mulungu (c) Mizimu yoipa (d) Chinthu china chochimwa chotchedwa 'Satana'.
3. Liwu loti 'Mdirekezi' palokha limanthauzani?
(a) Tchimo (b) Njoka (c) Wonamiza moyerekeza / Wodetserera (d) Lusifala
4. Liwu loti 'Satana' palokha limanthauzani?
(a) Wochimwa (b) Wotsutsa (c) chirombo (d) Mfumu ya ma 'demoni'
5. Kodi liwu loti 'Satana' lingawiritsidwe ntchito ponenanso za anthu ochita zabwino?
6. Mophiphiritsa, mawu oti 'Satana' ndi 'Mdirekezi' angayimire chiyani?
7. Kodi liwu loti ma 'demoni' litanthauzani monga lagwiritsidwa ntchito m'Chipangano Chatsopano?
(a) Angelo ochimwa (b) Matenda (c) Chilankhulidwe chamasiku amenewo choyimira matenda, chimene anthu ankaganiza kuti ankayambitsa ndi ma 'demoni' (d) Mizimu
8. Mudziwanji za njoka ya mmunda wa Edeni?

Mukayankha mafunso'wa chonde tumizani ku imodzi mwa ma adiresi mwapatsidwa m'mapeji oyambirira a buku lino.

PHUNZIRO 7

CHIYAMBI CHA YESU

7.1 UNENERI WA YESU M'CHIPANGANO CHATSOPANO

Phunziro 3 tinawerenga za cholinga cha Mulungu pa chipulumutso chatu ife anthu, ndipo kuti izi zayimanso pa maziko okhazikidwa mwa Yesu Khristu. Malonjezano amene Mulungu anapanga ndi Heva, Abrahamu komanso Davide, onse akunenapo za Yesu ngati mphukira yawo. Ndizoonadi kuti Chipangano chonse Chakale chinalosera za kubwera ndinso uneneri wanzeru wa Yesu Khristu. Lamulo la Mose, limene Israeli ankayenera kutsata ndinso kulimvera Yesuyo asanabadwe, linkakamba pafupi pafupi za kudza kwa Mesiya kotero, “...*Chilamulo chidakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Khristu*” (Agalatiya 3:24). Nchifukwa chake, panyengo ya Paskha, mwana wa nkhusa oyenera, opanda banga ndi chilema chilichonse anayenera kuphedwa (Eksodo 12:3-6); Izi zinkayimira nsembe ya Khristu, “*Mwana wankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi*” (Yohane 1:29; 1 Akorinto 5:7). Ungwiro wa Mwana wankhosa udayenera kuonedwa bwino pamene munthu ankafuna kupereka nsembe, popeza nsembeyo inkayimira nsembe ya ngwiro yomwe idaonetsedwa mchikhalidwe ndi kudzipereka kwa Yesu (Eksodo 12:5 cp. 1 Petro 1:19).

Tikamawerenga mabuku a Masalmo ndi Aneneri a m'Chipangano Chakale, timamva zambiri zokhudza m'mene Mesiyo angadzachitire zinthu zonse. Mabuku amenewa amanenanso za chikhalidwe cheni cheni cha Mpulumutsiyo. Timamvanso m'mene Mesiya anayenera kubadwa, kuzunzika ndinso kufa imfa yamanyazi pamtanda. Ngati lero lino a chipembedzo cha chi Yuda amakanabe kuti Mesiya anali Yesu, ndipo kuti adayenera kufa monga Yesu anachitira; Izi zimaonetseratu kusamvetsa kwa munthu ndikunyozeru kumene kwabwera chifukwa cha tchimo lomwe liri pakati pathu ngakhale timawerenga Mau Opatulika. Ndime ziri m'munsizi zikutionetseratu momwe munthu wasokonezera chikhulupiriro.

Uneneri M'Chipangano Chakale:

“Mulungu wanga, Mulungu wanga mwandisiyiraji ine?” (Masalmo 22:1).

“Chitonzo cha anthu, ndi wonyozedwa ndi anthu. Onse akundipenya andiseka: Akwenzula, napukusa mutu, naati, Adadzitengera kwa Yehova; kuti adzampulumutsa, Amlanditse tsopano popeza akondwera naye.” (Masalmo 22: 6-8).

“Ndi lirime langa likangamira ku nsaya zanga;Andiboola m'mapazi anga,” (Masalmo 22:15, 16).

Onaninanso kuti Masalmo 22:22 akuloserwa kwambiri nkhani imene Yanenedwanso poona m'buku la a Hebri:12.22.

“Abale anga andiyesa mlendo, Ndi ana a mai wanga andiyesa wa mtundu wina. Pakuti changu cha pa nyumba yanu chandidya; Ndi zotonza za iwo otonza Inu zandigwera ine” (Masalmo 69:8,9).

“Agawana zobvala zanga, Naalota maere pa malaya anga” (Masalmo 22:18)

Kukwaniritsidwa kwa Uneneri M'chipangano Chatsopano

Awa ndi mau amenenso Yesu ananena pamtanda pamene adapachikidwa (Mateyu 27:46).

Israeli ananyoza Yesu ndi kumnyogodola (Luka 23:35; 8:53); anapukusa mitu yawo (Mateyu 27:39), ndipo ananena zonsezi Iye atapachikidwa pamtanda (Mateyu 27:43).

Ulosi uwu unakwaniritsidwa pamene Khristu anamva ludzu pamtanda paja (Yohane 19:28). Kuboola manja ndi mapazi kunachitikadi pamene Khristu ankapachikidwa pamtanda ndipo anamukhomera misomali m'manja ndi mapazi.

Kukwaniritsa kweni kweni kwa uneneri uwu kukupezeka pa Mateyu 27:35.

“Ndipo anandipatsa ndulu ikhale chakudya changa; Nandimwetsa vinyo wosasa pomva ludzu ine” (Masalmo 69:21).

Nunsu imeneyi iwonetseratu chithunzi thunzi cha Yesu Khristu pamene a Yuda kuphatikizapo abale ake eni eni ankamukana. (Yohane 7:3-5; Mateyu 12:47-49). Izi zakambidwanso pa Yohane 2:17.

Zinthu zimenezinso zinaonekadi Khristu Yesu atangopachikidwa pamtanda paja. (Mateyu 27:34).

Tikawerenga buku lonse la Yesaya 53, tiona kuti pakupezeka uneneri wamphamvu zedi pankhani yokhudza za imfa ya Khristu ndi kuukanso kwa Yesuyo kwa akufa. Ndime iriyonse ya gawo limeneri la Yesaya, likufotokoza chindunji cheni cheni cha Yesu chimene chinakwaniritsidwa m'Chipangano Chatsopano.

Werengani zitsanzo m'ndime ziwiri ziri m'munsizi:

“Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pake; ngati nkhosa yotsogoleredwa kophedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali duu pamaso pa onsenga, motero sanatsegula pakamwa pake” (Yesaya 53:7).

“Ndipo anayika manda ake pamodzi ndi oyipa; ndi pamodzi ndi olemera muimfa yake, ngakhale Iye sanachita chiwawa, ndipo mkamwa mwake munalibe chinyengo” (Yesaya 53:9)

Khristu, mwana wankhosa wa Mulungu, anakhala chete pa

nyengo imeneyi ya m'nyozo ndi mayesero a mphamvu ngati kuti sanamve kuwawa. (Mateyu 27:12,14).

Yesu anapachikidwa pamtanda pamodzi ndi anthu akuba komanso zigawenga (Mateyu 27:38) Ngakhale kuti anayikidwa m'manda a munthu wolempera, Iye sanalemekezeke (Mateyu 27:57-60)

Sizodabwitsa choncho, kuona kuti Chipangano Chatsopano chikutikumbutsa za ***“Chilamulo ndi Aneneri”*** a m'Chipangano Chakale, kuti ndicho ngodya

ndi maziko eni eni amene atizindikiritsa za Khristu Yesu (Machitidwe 26:22; 28:23; Aroma 1:2,3; 16:25,26). Yesu Mwini ananenetsa kuti ngati sitizindikira **“Chilamulo ndi zolembedwa ndi Aneneri”**, sitidzamva ndi kumulola Iye (Luka 16:31; Yohane 5:46,47).

Kunena za chilamulo cha Mose kuti chinalosera za Khristu, ndikutinso aneneri ankalosera za kubwera kwa Iye Yesu, ndicho chinthu chimene chingatitsimikizire mosabvuta za Baibulo kuti ndi Mau a Mulungu. Ndipo kuti zikutionetsanso poyera motsimikiza mfundo yoti Yesu kudalibe kalelo mpaka pamene adabwera pobadwa mwa Maria namwaliyo. Ulaliki wopanda gwero umene uli wabodza, onena za Yesu kuti adalipo kale pa chiyambi cha chilengedwe, sungatilimbikitse m’chikhulupiriro cheni cheni pakati pathu, maka maka tikamaganizira za malonjezano amene amabwerezedwa bwerezedwa kuti Iye adzakhala Mbeu ya Heva, Abrahamu ndi Davide. Tikanena kuti Yesu adaalipo kumwamba pamene Yehova ankapanga malonjezano amenewa, tikhala ngati tikunena kuti Mulungu ananama popeza Yesuyo analipo kale. Koma apa Mbeu yawo yawo (yobadwa mwa iwo) ndi imene inkalonjezedwa osati imene idaalipo kale ayi. Potero, Mulungu ananenetsa kuti anthu amenewa adzakhala ndi mwana (osati ana), Mbeu yawo yawo yobadwa mwaiwo eni amenenso akanadzakhala Mesiya - Mpulumutsi. Tikawerenga za magwelo ndi mfuko la Yesu Khristu mu Mateyu 1 ndi Luka 3, timamva kuti Yesu anabadwa kwa makolo ake ndipo makolo omaliza akuthera pa anthu oyambirira amenewa, omwensho ndi amene Mulungu adapangana nawo pa malonjezano akubadwa kwa Yesu Khristu.

Lonjezo la kwa Davide posimba za Khristu, silikunena kuti Yesu adalipo kale kumwamba pamene lonjezoli linkapangidwa ndi Mulungu kwa Abrahamu kapena Davide ayi: **“...Ine ndidzaukitsa mbeu yako pambuyo pako, imene idzatuluka m’matumbo mwako, ndipo ndidzakhazikitsa ufumu wake..Ndidzakhala Atate ake, iye nadzakhala mwana wanga”** (2 Samueli 7:12,14). Muonetsetse kuti apa nkhanayi inkakambidwa pofotokoza za zinthu zodzachitika mtsogolomo. Tikaona kuti Mulungu ndi amenenso akanadzakhala Atate wa mwanayo, zikutitsimikiziradi kuti mwanayo kudalibe kwina kulikonse poyambapo. Ponena kuti mwanayo akanachoka m’matumbo mwa Davide, zikuonetsanso kuti adayenera kukhala mwana weni weni ochokera m’thupi la Davide. **“Yehova analumbira Davide zoono; sadzalibweza; ndi**

kuti waiwo okhala zipatso za m'thupi lako ndidzayika pampando wa chifumu wako,” (Masalmo 132:11).

Solomo anaali mwana amene anakhala ngati wakwaniritsadi lonjezolo, koma pamene Mulungu ankapanga lonjezo limeneri, nkuti Solomo atabadwa kale (2 Samueli 5:14), choncho, sadali Solomoyo ayi. Kukwaniritsidwa kweni kweni kwa lonjezo la mwana wobadwa mwa Davide amenenso akanakhala Mwana wa Mulungu kotero, kuyenera kukhala kuti kunaali kubadwa kwa Yesu Khristu (Luka 1:31-33). “...*ndidzamuukitsira Davide Mphukira wolungama, Iye adzakhala Mfumu*” mwachitsanzo, Mpulumutsi (Yeremiya 23:5).

Nkhani yokamba za mtsogolo m'mabuku a aneneri ena, amakambanso za Khristu. “*Ndidzawaukitsira* (ana a Israeli) *m'neneri wa pakati pa abale awo, onga iwe* (Mose);” Mau amenewa anenedwanso m'Machitidwe 3:22,23, ndime imene ikutiunikira pofotokozeru liwu loti “*Mneneri*” kunena za Yesu. “...*taonani, namwali* (Maria) *adzayima nadzakhala ndi Mwana wamwamuna, nadzamutcha dzina lake Imanueli*” (Yesaya 7:14). Ichi chinakwaniritsidwadi pamene Khristu anabadwa (Mateyu 1:23).

7.2 KUBADWA MWA NAMWALI

Pamene tikuwerenga za kubadwa kwa Yesu mwa mdzakazi, sizonetsa chirichonse chomwe chingatsimikizire kuti Yesu adaalipo kale ayi. Amene amakhulupirira kuti kuli milungu itatu mwa m'modziyo, amanena kuti nthawi ina kudaali milungu itatu kumwamba, mulungu wina anangosowa ndipo ndi amene adapezeka kuti ali mwa Maria pamene Mariayo adakhala ndi pakati. Taphunzira kale kuti Baibulo limanena kuti chinthu china chirichonse chidapangidwa mu uthunthu wake ndipo chili ndi chiyambi chake. Ngakhale Mulungu mwini alinso mu uthunthu (image) wake omwe ndi ofanana ndi munthu koma kuti Iye Mwini alibe chiyambi chake. Izi ndi zimene timawerenga m'Baibulo osati zoganiza munthu ayi. Lero anthu amanena kuti Yesu adaalipo kalero, ndipo kuti uthunthu wake unabwera kuchoka kumwamba nkulowa mwa Maria. Maganizidwe ndi ulaliki wotere ndi zimene sizikupezeka pena paliponse m'Baibulo. Baibulo likutiuzza kuti Yesu anabadwa

mwa Maria namwaliyo osati kuti adalowa mwa Maria ayi. Mbiri ya chiyambi cha Khristu Yesu, siyinenapo kanthu kena kalikonse kotiganizitsa kuti Yesu anayamba atakhalapo mu uthunthu wake asanabadwe ayi. Ndipo Mau a Mulungu sanakambepo china chirichonse chowonetsa kuti Yesu anachoka kumwamba nalowa mwa Maria ali mu uthunthu wakewo ayi. Kotero, popeza palibe umboni kapena ndime imene imafotokoza za mfundo imeneyi ya milungu itata m’Baibulo, kwaife ndikobvuta kulalikirira zinthu za bodza ngati zimenezi.

“Mngelo Gabrieli anaoneka kwa Maria ndi uthenga woti:
“Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamutcha dzina lake Yesu. Iye adzakhala Wamkulu, naadzatchedwa Mwana wa Mkulukulu:....Koma Maria anati kwa m’ngelo, Ichi chidzachitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna? (mwachitsanzo, anali buthu losadziwa mwamuna). **Ndipo m’ngelo anayankha naati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi Mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe, Chifukwa chakecho, choyeracho chikadzabadwa, chidzatchedwa Mwana wa Mulungu”** (Luka 1:31-35).

Tamva apa kawiri konse kuti Yesu akadzabadwa, adzatchedwa Mwana wa Mulungu; kuonetseratu kuti Mwana wa Mulunguyo, kunalibe, anali asanabadwe; mwachitsanzo, **“adzakhala Wamkulukulu”**. Akanakhala kuti Yesu adalipo kale pamene mngeloyo ankalankhula mau amenewa, ndiye kuti akanakhala ali Wamkulukulu kale, sikukanayenera kwa Iye kuti achite kusandulika kuti akhale Wamkulukulu ayi. Yesu Khristu anali **“Mwana wobadwa yekha”** m’banja la Davide (Chibvumbulutso 22:16), Liwu la chi Greek limene linanthauzidwa kuti **“Mwana”** m’ndime imeneyi, ikutsimikiziradi kuti anali Mwana weni weni wofumira mfuko la Davide.

CHIYAMBI CHAKUBADWA KWA YESU

Kudzera m’mphamvu ya Mzimu Woyera (mpweya/mphamvu ya Mulungu) imene inawuziridwa nimufika Maria; Iye anakhala ndi pakati ngakhale kuti anali asanadziwane ndi mwamuna aliyense. Choncho, n’chifukwa chake Yosefe sadali bambo wake weni weni wa Yesu. Tiyenera timvetsetse pano kuti Mzimu Woyera simunthu kapena chinthu china chamoyo chodziyendera chokha ayi (Phunziro 2); Yesu adali Mwana wa Mulungu, osati mwana wa Mzimu Woyera. Pogwiritsa ntchito Mzimu wake Woyera, Mulungu

anamuphimba Maria, “*Chifukwa chakenso choyeracho*” chimene chinabadwa mwa iyeyo “*chinatchedwa Mwana wamwamuna wa Mulungu*”(Luka 1:35). Mau oti “*chifukwa chakenso*” akuonetsa poyera kuti pakanapanda Mzimu Oyera, kumfika Maria, Mwana wa Mulungu sakanakhalapo koteronso, ife lero sitikanatha kukamba kanthu za Iye.

Kuti Yesu anachita kubadwa mwa Maria (Luka 1:31) ndi chitsimikizo chapadera chimene chinawonetsera kuti Khristu sadalipo kuchokera pachiyambi. Munthu akakhala ndi pakati sizitanthauza kuti chimene chiri mwa iyeyo chachita kulowa mthupi mwakemo ayi, koma kuti thupi lake labvomereza ntchito imodzi ya chilengedwe kotero kuti, umoyo wamunthu wina ukuyambika mthupi lakelo. Moteronso, umoyo wa Yesu Khristu unachita kuyamba mwa Maria koma osati chifukwa chakuti Maria anakumana ndi mwamuna ayi, koma mwa Mphamvu ya Mulungu yopanda malire. Maria anakhudzidwa ndi mphamvu yosatha ya Mulungu. Yohane 3:16, ndime imene iri yotchuka kwambiri m’Baibulo, ikunena kuti “*Mwana Wake Yekhayo*” wa Mulungu. Mazana mazana a anthu amaloweza ndime imeneyi koma samatha kufotokozera bwino tanthauzo lake leni leni. Iwo samathanso kudzikhuthula m’malembo oyera amenewa kotero athe kuwazindikira m’magonero mwake mweni mweni. Ngati ‘*Yesu anabadwa yekha*’ ndiye kuti anachita ‘*kuyamba*’ kukhala ndi moyo pamene Maria anakhala ndi pakati basi. Ndipo ngati Yesu anabadwa yekha mwamphamvu ya Mulungu ngati Bambo Wake, ziyenera kutilimbisa ife kuti Mulungu wathu ndi wamphamvudi. Moteronso, kuti Mulunguyo ndiyedi ‘*Wamkulukulu*’ kuposa Yesu Mwana wakeyo; nchifukwa chake, Mulungu alibe chiyambi (Masalmo 90:2) choncho, Yesu sangakhalenso Mulungu (onani Phunziro 8 lomwe lakamba zambiri za izi).

Nzodziwikiratu kuti Yesu “*anabadwa yekha*” modzozedwa ndi mphamvu ya Mulungu, osati kuti analengedwa pachiyambi monga Adamu ayi. Izi zikuonetsa kuti Mulungu ndi Yesu Khristu sanatalikirane – “*Mulungu anali mwa Khristu ali nkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye Yekha*” (2 Akorinto 5:19). Pamene timva kuti Yesu anabadwa payekha osati kuchita kulengedwa kuchokera m’nthaka monga Adamu ndi Heva, zionetsera kuti chikonzero chinalipo ndi Mulungu kalelo kuti adzapezadi njira ina yotipulumutsira ife kupsinjo ya machimo yomwe mphotho yake ndi imfa.

Yesaya 49:5,6 timawerenga ulosi wokhudza za Khristu kuti ali ngati **“kuunika kwa dziko lapansi”** kumene Yesuyo anakwaniritsa pogonjetsa imfa (Yohane 8:12). Iye akambidwa ngati **“Ambuye amene anandiumba ine kuchokera m’mimba mwa mayi kuti ndikakhale kapolo wake”** Khristu kotero, **‘anaumbidwa’** ndi Mulungu m’mimba mwa Maria, kudzera m’Mphamvu ya Mzimu Woyera. M’mimba mwa Maria kotero, ndiwo malo amene tonse tiyenera kudziwa, chiyambi cheni cheni cha Yesu Khristu.

Taphunzira kale m’Phunziro 7.1 kuti Masalmo 22 akulingalira kwambiri za maganizo a Khristu pamene adzakhale pamtanda. Iye analingalira motere: **“m’nandichotsa ine kuchokera m’mimba mwa mayi wanga.....Inu ndinu Mulungu wanga kuchokera mmimba mwa mayi wanga”** (Masalmo 22:9,10). Ndipo pamene Yesu ankafa pamtanda, Iye anayang’ananso m’mbuyo pa chiyambi cha moyo wake, nakumbukira kuti anabadwa kuchokera m’mimba mwa mayi wake Maria, popangidwa ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera yomwe ndi yochokera kwa Mulungu. Choncho, kungokamba za Maria mu **‘Uthenga Wabwino’** kuti ndiye adali ‘mayi’ wake wa Yesu, zikutsekeratu maganizidwe a bodza onena kuti Yesu adalipo kale Iye asanabadwe mwa Maria’yo.

Maria adali munthu wamba, ndipo monga anthu ena onse, adalinsu ndi makolo ake. Tikhoza kuona kuti adali ndi msuweni wake yemwensu anabereka Yohane m’Batizi, munthu wambanso monga anthu ena onse (Luka 1:36). Tikuonanso kuti zikutsutsana kwambiri ndi ulaliki wa chi Katolika onena kuti Maria sanali munthu wamba koma uthunthu osiyana ndi wa anthu wamba. A Katolika amasiyanitsa anthu ndi Maria ponena kuti Maria’yo sanafe koma kuti anawuluka napita kumwamba. Izi ndi zomwe sizikugwirizana ndiponso sizikutsimikizira zomwe zinalembedwa m’Baibulo kuti ngakhale Yesu **“anali Mwana wa munthu”** komanso **“Mwana wa Mulungu”**. Awa ndiwo maudindo opatsidwa kwa Yesu Khristu m’Chipangano chonse Chatsopano. Yesu adali **“Mwana wa munthu”** chifukwa anabadwa mwa Maria yemwe adali munthu; ndipo adali **“Mwana wa Mulungu”** chifukwa anabadwa ndi Mphamvu ya Mulungu mwa Maria chomwecho, Mulungu ndiye Atate wake. Izi sizingatheke ndipo tiona kuti sizingagwirizane bwino chomwechi ngati Maria akadakhala ndi uthunthu wina wapadera osafanana ndi munthu wamba. Ndiye kuti sadakakhala munthu monga timawerengera m’Baibulo. Uku nkutsutsanadi ndi Baibulo lomwe ndi mau a Mulungu.

“Adzatulutsa choyera m’chinthu chodetsa ndani? Nnena m’modzi yense. Munthu ndani kuti akhale woyera, Iye wobadwa mwa mkazi kuti akhale wolungama?...akhala bwaji wolungama wobadwa mwa mkazi?” (Yobu 14:4; 15:14; 25:4). Zonsezi zikutipatsa chithunzi chakuti Maria komanso Yesu sanabadwe ndi matupi kapena uthunthu wina wapadera osiyana ndi ife anthu wamba ayi.

Monga ife tinabadwa mwa mkazi, nayenso Maria sanasiyane ndi ife. Anabadwa mwa mkazi, ndi uthunthu wamachimo monganso ife, omwense Yesu anabadwa nawo onga a ife obadwa mwa mkazi. Yesu *“anabadwa mwa mkaziyo”* (Agalatiya 4:4). Popeza tamva kuti Yesu anabadwa mwa mkazi, ndi chitsimikizo chokwanira kuti anali ndi uthunthu komanso thupi la uchimo lomwense ndi lofanana ndi ife anthu wamba chifukwa anali *“wobadwa mwa mkazi”* ngati ife anthu wamba.

Pafupi pafupi, timawerenganso ndime zambiri m’Baibulo zoonetsa kuti Maria anali munthu wamba monga ife tiliri komanso mwina ife tili bwinopo m’miyoyo yathu padziko. Yesu anadzudzulidwapo kangapo chifukwa choonetsa poyera kufooka kwake mu zinthu za uzimu (Luka 2:49; Yohane 2:4); anthu ena anaonetseratu kuti sankamvetsa kawiri kawiri matanthauzo a zimene Iye Yesu ankalalikira (Luka 2:50). Izi ndizimene tiyenera kuyembekezera kuchitika kwa munthu wamba ngati Maria ngakhale kuti mwana wake Yesu anali Mwana wa Mulungu monganso adali mu umunthu ngati ife lero. Mwaichi, timamva kuti Maria anakwatirana ndi Yosefe amenenso anali munthu ngati ife (Mateyu 1:25).

Tikhoza kutsimikizira izi pamene tingawerenge kuti Khristu anali ndi *‘Mayi ake ndi azichimwene ake’* (Mateyu 12:46,47);- choncho, tidziwa kuti Maria adalinso ndi ana ena pamwamba pa Khristu Yesu. Koma tidziwense kuti Yesu anali *“Mwana wake woyamba”*. Sititha kumvetsa pamene a Katolika amafika mpaka ponena kuti Maria anakhalabe mdzakazi atabadwa Yesu mpaka anakwera kumwamba chifukwa ulaliki umenewu sitingaupeze m’Baibulo, ndipo kuti zikutsutsana ndi zimene zidalembedwa m’Mau Oyera. Tikunena pano kuti palibe anakwera kumwamba koma Yesu yekha (Yohane 3:13); kotero, ngati Baibulo likunena chonchi, ndiye kuti Maria ayenera kuti anakalamba namwalira. Titsimikizirane kotero, pano kuti ngati Khristu anali mu uthunthu ndi umunthu monga ife (A Hebri 2:14-18; Aroma 8:3)

zitanthauzanso kuti Maria adali chimodzi modzi; mwaichi, sanalinso osiyana ndi anthu ena alionse ayi.

7.3 UDINDO WA KHRISTU MCHIKONZERO CHA MULUNGU

Mulungu safanana ndi munthu, amene amati akaganiza kuchita chinthu mwandondomeko ina yake, amathanso kusintha nkuchita mosiyana ndi chikonzero choyambacho. Nchifukwa chake, kusiyana kwa ife ndi Mulungu kumaoneka pamene tiganizira za chikonzero chake cha Chiuta. Mulungu anayika kale chikonzero chonse cha chilengedwe pachiyambi (Yohane 1:1). Maganizo ake okhala ndi Mwana kotero, adalipo kuchokera pachiyambipo. Tikawerenga ziphiphiritsa za m'Chipangano Chakale, tiona kuti chikonzero chimenechi chidali chodziwikiratu pamaso pa Mulungu; chikonzero cha chipulumutso kudzera mwa Khristu Yesu.

Taonetsa kale pokamba za malonjezano, maulosi a aneneri, mitundu ya Malamulo a Mose kotero, tikamawerenga zimenezi m'Chipangano Chakale, timaona cholinga cha Mulungu akubwera kwa Khristu Yesu. Timamvanso kuti chinali chikonzero cha Mulungu kuti m'maganizo mwake, Mwana wake Yesu analipo kuchokera pachiyambi cha chilengedwe (A Hebrai 1:12). Chinali chodziwika mwa Khristu kuti mbiri ya munthu padziko lapansi ndiyo ndondomeko yokonzedwa ndi Mulungu (A Hebrai 1:2). Mwaichi, zikugwirizana kuti Chipangano Chakale chikukambadi zambiri zokhudza munthu m'chikonzero cha Mulungu kudzeranso mwa Khristu Yesu.

Ukulu wa Yesu ndi kufunikira kwake pamaso pa Chiuta ndichinthu chimene ife sitingachimvetsetse ngati sitifatsa bwino ndi Baibulo. Choncho, nzowona kuona kuti Yesu Khristu adalipo m'maganizo ndi mumtima mwa Mulungu pakuyamba kwa chilengedwe ngakhale kuti Yesuyo adali asanabadwe koma adaonekera kwaife pamene anabadwa mwa Maria namwaliyo. A Hebrai 1:4-7, 13, 14 akutsindika kuti ndithu Khristu, sanali m'ngelo; ndipo kuti pamene anabadwa mwamunthu, adali ndi mphamvu zochepa kuyerekeza ndi zimene

angelo adali nazo (A Hebri 2:7); kenaka, anakwezedwa kuposa iwo angelowo powona kuti anali *“Mwana wa Mulungu wobadwa yekha”* (Yohane 3:16). Taonetsa kale kuti njira yokhayo yomwe munthu ndi Yesu adali nayo ndiyo mu uthunthu ndi umunthu omwe siunali ofanana kweni kweni ndi Mulungu, choncho, Khristu sanakhalepo ngati *‘Mzimu’* asanabadwe. 1 Petro 1:20 akunena izi mwachidule motere: Khristu *“amene anadzozedwa dziko lapansi lisanakhazikitsidwe koma anaonetsedwa mu umunthu weniweni masiku omalizawo”*. Yesu ndiye chikatikati cha Uthenga Wabwino, chimene Mulungu *“analonjeza kudzera mwa aneneri ake m’Mau Oyera wakunena za Mwana wake, amene anabadwa wa Mbeu ya Davide, monga mwa thupi, amenenso anatsimikizidwa ndi Mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa Chiyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Khristu Ambuye Wathu;”*

Apa tsopano tiona kuti chifupikitso cha mbiri ya Khristu ndicho:

1. Analonjezedwa m’Chipangano Chakale – m’maganizo ndi Mau a Mulungu.
2. Analengedwa pobadwa mwa mdzakazi ngati mbeu ya Davide.
3. Chifukwa cha chilungamo ndi kuyera mtima kwake, mwa Mzimu Woyera m’moyo wake pa dziko lapansi,
4. Anaukitsidwa, ndipo pamaso pa anthu, anatchulidwa Mwana wa Mulungu ndi akuphunzira ake polalikira za Iye motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

NZERU ZODABWITSA ZA MULUNGU

Tingathandizike komanso kukhutitsidwa pamene timvetsetsa ndi kuzindikira kuti Khristu anali mmaganizo mwa Mulungu ngakhale kuti adali asanabadwe. Ichi n’chifukwa chakuti Chiuta amadziwa zonse zakutsogolo kwathu pamene ife maganizidwe athu sangathe kumvetsa chinsinsi chimenechi. Choncho, Mulungu akhoza kufotokoza zamtsogolo; akhoza kukamba komanso kuganizira za kutsogolo kwa munthu nakamba ngati kuti zinthu zochitika kutsogolozo zachitika kale kapena kuti zikuchitika kumene. Izi ndizo Mphamvu, Nzeru ndi kuzizwitsa kwa Mulungu Yehova monga timawerengera. Mulungu *“...aitana zinthu zoti palibe monga ziripo”* (Aroma 4:17). Atha kunena kotero, kuti *“...ndilalikira za chimalizo kuyambira pa chiyambi, ndikuyambira nthawi zakale ndinena zinthu zimene zisanachitidwe; ndikunena, Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzachita zofuna zanga*

zonse;” (Yesaya 46:10). Chifukwa chaichi, Mulungu amalankhula za anthu ngati kuti ali moyo kale ngakhale kuti anthuwo asanabadwe.

“*Uphungu*” kapena kuti Mau a Mulungu, analosera za Khristu pachiyambi ngakhale kuti Yesu anali asanabadwe; Iye adali mu cholinga ndi chifuniro cha Yehova. Nchodziwikiratu kotero, kuti Khristu zikanatheka kubadwa nthawi ina iriyonse; ndipo Mulungu akanakwaniritsa cholinga ndi chifuniro chimenecho mwa Khristu’yo. Pano tiona kuti nzeru ndi ungwiro wa Mulungu zimaonekera makamaka pamene Mau ake komanso maganizo ake amene adawanena kalelo akwaniritsidwa pamaso pa anthu amene adawamva mau’wo. Timaona kuti mu chi Heberi mau a ulosi kapena tinene kuti uneneri amafotokozedwa ngati kuti zinthuzo zinachitika kale ngakhale kuti ndi zinthu zomwe ziyenera zidzachitike kutsogolo. Nchifukwa chake Davide ananena, “*Iyi ndi nyumba ya Yehova Mulungu*” (1 Mbiri 22:1 – onani kuti Baibulo la Chichewa silinamasulire bwino); nthawiyi nkuti kachisiyo asanamangidwe. Timvetse kuti ngakhale kuti Mulungu anakamba za nyumba polankhula mwa Davide, nyumbayo idali isanayambe kumangidwa kotero, ananena izi popeza chinali chilankhulo chachi Yuda nthawiyo ndipo kuti Mulungu anafuna kulimbikitsa chikhulupiriro chawo polankhula m’chilankhulo chawo chodziwika pakati pawo. Ichi, ndicho chikhulupiriro chawo pamaso pa Chiuta. Mau Opatulika akutipatsa zitsanzo zambiri zokhudza momwe Mulungu amagwiritsira ntchito nzeru zake zochuluka pakati pa anthu ake. Yehova anatsimikizira kuti adzakwaniritsa malonjezano amene anapangana ndi Abrahamu namuza: “*Ndapatsa mbeu yako dziko ili*” (Genesis 15:18) pamene Abrahamu’yo analibe mwana ndi m’modzi yemwe. Ndipo panthawi yomweyi Isake asanabadwe, Mulungu analonjezanso: “*Ndakupanga iwe kukhala tate wa mitundu ya mayiko ambiriwo*” (Genesis 17:5). Apa tiona kuti Mulungu anakamba za zinthu zimene palibe ngati kuti zilipo.

Khristu anafotokozapo pamene ankafalitsa Uthenga Wabwino za momwe Mulungu “*anampatsa zinthu zonse m’dzanja lake*” (Yohane 3:35), ngakhale kuti sizinali choncho panthawi imeneyi ndipo mpaka pamene anafa pamtanda paja kugonjetsa imfa. “*Mudagonjetsa zonse panso pa mapazi ake....Koma sitinayamba tsopano apa kuona zonse zigonjera*” (A Heberi 2:8).

Mulungu analankhula za mapulani ndi zolinga za chipulumutso kudzera mwa Yesu “*ndi mkamwa mwa aneneri ake oyera mtima, akale omwe, pamene*

dziko linayamba” (Luka 1:70). Chifukwa chakuti aneneriwa ankakhudziwa kwambiri ndi chikonzero cha Mulungu, iwo anakambidwa ngati kuti analipo dziko lisanayambe ngakhale kuti tikudziwa, iwo onse kunalibe pamene dziko linkalengedwa. M’ malo mwake, tikhoza kunena kuti aneneri adalipo m’ maganizo ndi mchikonzero cha Mulungu kuchokera pachiyambi. Yeremiya ndi chitsanzo china chachikulu komanso chapadera. Mulungu anamuza iye: **“Ndinakulenga iwe m’ mimba mwa mayi wako, ndinakudziwa iwe , ndipo usanabadwe ndinakupatula iwe; ndipo ndinakudzoza ukhale m’ neneri”** (Yeremiya 1:15). Kotero, Mulungu anadziwa zonse zimene Yeremiya ankachita ngakhale kuti Yeremiya’yo anali asanabadwe, ndipo ngakhale chilengedwe chisanachitike ndi Chiuta, Iye Mulungu anadziwa zonse za Iye. Mwanjira imeneyi Mulungu anathanso kunena za Koresi wa ku Persia angakhale kuti Koresiyo anali asanabadwe. Komanso kuti polankhula Yehova anakamba ngati kuti Koresiyo analipo kale panthawiyo (Yesaya 45:1-5). A Hebrai 7:9,10 ndi chitsanzo china chopezekeratu pa kakambidwe konena za munthu kuti alipo ngakhale kuti panthawiyo munthuyo ankakhala kuti sanabadwe.

Mnjira yomweyi, monga Yeremiya ndi aneneri enawo akambidwa ngati kuti analipo chilengedwe chisanachitidwe chifukwa cha mbali yomwe iwo adali nayo pa chikonzero cha Mulungu, anthu olungama nawonso adakambidwanso ngati kuti adalipo pamene iwo adali asanabadwe. Kotero ife okhulupirira tonse tidalipo m’ maganizo a Mulungu ngakhale kuti mthupi, tinali tisanalengedwe. Mulungu **“...amene anatipulumutsa ife, natiitana ife ndi maitanidwe oyera, simonga mwa ntchito zathu, komatu monga mwachitsimikizo....ndi cholinga mchisomo chake, chopatsidwa kwaife mwa Khristu Yesu zisanayambike nthawi zoyamba”** (2 Timoteo 1:9). Mulungu **“anatisankha ife mwa Iye (mwa Khristu) lisanakhazikike dziko lapansi,...anatifotokonzera ife njira ya chiyero....monga umo kunakomera Iye mwa chifuniro Chake** (Aefeso 1:4,5). Chithunzi thunzi chonse cha Mulungu pa anthu onse, yense payekha payekha kukukambidwa ndi Mulungu pachiyambi, ndi kuti ndiko **“kusankhidwa mwapadera”** ku chipulumutso zomwe zikuonetsa kuti zonsezi zidalipodi m’ maganizo a Mulunguyo pachiyambi cha chilengedwecho (Aroma 8:27; 9:23).

Mkuzindikira izi, nzosadabwitsa kuwona kuti Khristu, ngati chifupikitso cha cholinga cha Mulungu, anakambidwa ngati kuti adalipo kuchokera pa

chiyambi m'maganizo ndi chikonzero cha Mulungu, ngakhale kuti sadalipo pa nthawiyo. Iye adali *“mwana wa nkhosa wophedwa kuyambira makhazikitsidwe a dziko lapansi”* (Chibvumbulutso 13:8)

Yesu sikuti anafa nthawi imeneyi ayi, Iye *“anali mwana wankhosa wa Mulungu”* woperekedwa ngati nsembe yopsereza kwa zaka 4,000 zotsatirazo (1 Yohane 1:29; 1 Akorinto 5:7). Ndipo mwanjira yomweyi pamene Khristu anasankhidwa kuchokera pa chiyambi (1 Petro 1:20), okhulupirira onse nawonso anasankhidwanso (Aefeso 1:4; lomwe ndi liwu limodzi lomwelo m'Baibulo la chi Greek). Bvuto limene liripo lero lino ndi lakuti, anthu samamvetsa matanthauzidwe amenewa chifukwa chakuti mmitima mwawo muli kale maganizo osiyana ndi zimene Baibulo limanena, kotero, iwo samafunanso kuwerenga modekha kuti amvetse bwino ngakhale angauzidwe kutero. Chikhulupiriro cheni cheni ndicho kuyang'anira maganizo a Mulungu mchoonadi mosayang'ana nthawi yomwe ife tikufuna zilakolako zathu ngakhale nthawi italike bwanji. Komanso ngakhale zinthuzo zingachedwe bwanji.

7.4 “PACHIYAMBI PANALI MAU” YOHANE 1:1-3

“Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali ndi Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi kwa Mulungu. Zonse zinalengedwa ndi Iye” (Yohane 1:1-3).

Ndime zimenezi zikutsimikiziranso ndondomeko ya mau amene takambirana kale pamwambapa. Tiona kuti ndime tawerenga pa Yohane 1:1-3 ndiyomwensho anthu ena amasokonezeka nayo kwambiri kotero, amabweretsanso chisokonezo kwa anthu ena chifukwa samamvetsa bwino tanthauzo leni leni la ndime imeneyi. Izi zimachitika nthawi zinanso chifukwa anthuwo amafuna kukwaniritsa maganizo awo amene kawiri kawiri amasiyana ndi m'mene Baibulo limafotokonzera pa chikonzero cha Mulungu pokhudza ndimeyi. Iwo amalimbikira chiphunzitso chonama pomanena kuti Yesu adalipo kale kumwamba Khristu'yo asanabadwe. Tiyenera tizizindikira

kwathunthu matanthauzo eni eni a mavesi ngati amenewa. Mwachitsanzo, liwu loti **“mau”** m’ndime imeneyi litanthauza chiyani kuti ife tikhutire pamene tiwerenga ndimeyi ponena kuti **“panali Mau”** m’Baibulo? Mau amenewa sakukamba za munthu chifukwa munthu **“sangayandikire pafupi ndi Mulungu”** pamene munthuyo tikuti akhalenso Mulungu nthawi yomweyo; monga Yesu akuti analinso Mulungu. Liwu la m’chi Greek limene lamasuliridwa kuti *‘Mau’* pano ndi **“logos”** limene palokha mchilankhulocho silikutanthauza kuti Yesu kapena kukhudzanapo ndi tanthauzo la liwu lonena za Yesu. Nthawi zonse liwu limeneri (logos) limatanthauzidwa kuti **“Mau”** komanso m’ malo ena m’Baibulo limatanthauzidwanso ngati:-

chochitika	maganizo
mtokoma	ulaliki
cholinga	chipembedzo
chifukwa	zonenedwa
ndondomeko	uthenga ndi zina zotero

“Mau” apa akukambidwa ngati chinthu chamwamuna chifukwa liwu loti **“logos”** m’chi Greek linagwiritsidwa ntchito ngati liwu loyimira amuna. Koma izi sizitanthauza kuti liwu’li likuyimira za munthu wamwamuna monga Yesu ayi. Tikawerenga ma ‘version’ (kumasulira kwa chi Greek kapena chi German kosiyana siyana), mwachitsanzo, ma Baibulo a zilankhulo zina, nkumawerenga pamodzi mofananiza matanthauzo a mavesi, tiona kuti mau omwewo anamasuliridwa ngati a chikazi (i.e Luther version – **‘das wort’**; Segond version – **‘la parole’**) choncho, izi sizitanthauza kuti **‘Mau’** sanganene za amuna ayi.

‘PACHİYAMBI’

Liwu loti ‘logos’ likuyimira maganizo a Mulungu omwe anenedwa kale mwachindunji m’mau ake kwaife. Mulungu pa chiyambi adali ndi **Mau** amenewa. Ndipo cholinga chimenechi chidayima pa Khristu kuti ayenera kubadwa pakati pathu popeza padali chifukwa chachikulu. Tawonetsa kale momwe Mzimu wake unakwaniritsa maganizo ake a Mulungu mwakuchita chinthu – nchifukwa chake Mzimu wa Mulungu ndi Mau ake zonse nzogwirizana (onani gawo 2.2). Monga Mzimu wa Mulungu unagwira ntchito polimbikitsa anthu ake, tionanso anthuwo kuti anauziridwa ndikudzozedwanso ndi Mzimuwo kuti athe kulemba bwino Mau a Mulunguwo. Kuchokera pa ‘chiyambi’ kotero, zikulumikizana bwino ndi ganizo la Khristu pantchito yake

mogwirizana ndi *Mau* omwe anakwaniritsa m'maganizo a Mulungu apoyambawo. Khristu anali *logos* (Mau) a Mulungu, choncho, Mzimu wa Mulungu okambidwa mndondomeko ya Khristu unathandiza kukwaniritsa 'Mau' amenewa mwa Khristuyo. Nchifukwa chake, ndime zambiri m'Chipangano Chakale chimapereka chitsanzo chabwino cha Yesu Khristu chimene anthu ayenera kutengera pa ntchito zawo za tsiku ndi tsiku. Kotero, Khristu ndiye *Mau*; Anali cholinga cha Mulungu pachikonzero cha chipulumutso kudzera "m' Mau" kuyambira pachiyambi. *Logos* (potanthauza kuti 'mau') anagwiritsidwa ntchito kwambiri ponena za 'Uthenga Wabwino' wa Yesu Khristu, mwachitsanzo, *Mau a Khristu* (Akolose 3:16; cp Mateyu 13:19; Yohane 5:24; Machitidwe 19:10; 1 Atesalonika 1:8 etc). Dziwani kuti *Logos* anena za Khristu, osati za Iye ngati munthu wamba ayi koma za ntchito yake ndi uthenga wake. Pamene Khristu anabadwa, *Mau* anasanduka m'nofu ndi magari – '*Mau anasanduka thupi*' (Yohane 1:14). Yesu Iye Mwini anali "*Mau* (amene)*anasanduka thupi*" osati 'mau wamba' ayi; Iye anakhala *Mau* pobadwa mwa Maria osati panthawi ina iriyonse imene Mulungu anaganiza za Mau'wo ayi. Ndinthawi yokhayo imene Yesu anabadwa potero, anasandukadi kukhala *Mau osandulika thupi* osati kale monga ena amanenera ayi. Izi ndizimene tikuwerenga m'Baibulo mozama komanso motsimikizira podzipereka.

Chikonzero chonse pa nthawiyo kotero, chikugwirizana ndi uthenga okhudza Khristu umene udali ndi Mulungu pachiyambi, koma unadzaonetsedwa kapena titi unaululidwa mu uthunthu wa Khristu Yesu (kapenanso tinene kuti mthupi la Yesu) ndiponso mopitiriza apa, mu Uthenga Wabwino wolalikidwa ndi Yesuyo mchirumika choyamba. Kotero Mulungu, ananena za Mau ake kwaife kudzera mwakubadwa kwa Khristu (A Hebrai 1:1,2). Nthawi zonse tiwerenga kuti Yesu anafotokozera za Mau a Mulungu ndipo kuti Khristuyo anachita machiritso ndi zozizwitsa mu Mphamvu ya Mau a Mulungu komanso molamulidwa ndi Mau a Mulungu, koteronso, Mulungu akadziwike naululika pakati pa anthu (Yohane 2:22; 3:34; 7:16; 10:32,38; 14:10,24). Paulo anamvera lamulo la Khristu kuti akalalike Uthenga Wabwino wa Iye '*kumayika konse*': "...*kulalikira kwa Yesu Khristu, monga mwa bvumbulutso la chinsinsi chimene chinabisika mwa nthawi zonse zosayamba, koma chaonetsedwa tsopano,...ndi kudziwitsidwa kwa anthu a mitundu yonse mwa malembo a aneneriwo,*" (Aroma 16:25,26 cp. 1 Akorinto 2:7).

Moyo wosatha udzatheka kuperekedwa kwa munthu chifukwa cha ntchito yabwino ya Khristu pamene munthuyo ayichita bwinonso (Yohane 3:16; 6:53); kotero, pachiyambi Mulungu adali ndi ganizo komanso cholinga ndi munthu kuti akhale ndi chikonzero choncho, akhale ndi moyo wosatha pozindikira kuti Yehova anapereka nsembe yake yopsereza kudzera mwa Khristu Yesu yemwe analipo m' mau ake kalelo. Chibvumbulutso chotere chinafikadi pamene Khristu anakwaniritsadi zonse maka maka pomwe Iye anabadwa naafa munga mwamalemba: *“...mchiyembekezo cha moyo wosatha, umene Mulungu wosanamayo analonjeza zisanayambe nthawi zosayamba; koma pa nyengo za Iye yekha anaonetsa mau ake mu ulaliki”* (Tito 1:2,3). Taona momwe Mulungu wakhala akunenera za aneneri ake kuti akhala alipobe kunthawi zonse zosatha (Luka 1:70) kudzera mwa omwe iwo anakamba, popeza mau'wo anali ndi Mulungu kuchokera pachiyambi koma anakwaniritsidwa m' nthawi imeneyo.

Zifanizo za Yesu zinakwaniritsa ulosi umene unakambidwa za Iye kuti; *“... Ndidzatsegula pakamwa panga ndi mafanizo; Ndidzaulula zinthu zobisika chiyambire kukhazikitsidwa kwake kwa dziko lapansi”* (Mateyu 13:35). Mwanjira imeneyi, *“Mau anali ndi Mulungu...pachiyambi”* ndipo kuti mau'wo anakhala *“thupi”* pamene Yesu Khristu anabadwa.

MAU ADALI MULUNGU

Tsopano tafika mbali yoti tiganizire kuti *“Mau adali Mulungu”* motani? Maganizo athu ndi zolinga zathu zimaonetsa umunthu wathu komaso zochita zathu kuphatikizapo momwe ife timachitira zinthu nthawi zambiri. *Ine ndikupita ku London* ndi mau kapena tinene kuti chidziwitso cha cholinga changa chifukwa ichi ndichimene ine ndachiganiza kuchichita. Cholinga cha Mulungu pakubadwa kwa Yesu Khristu kukutilunjikitsanso kuti ife timvetse pa nkhanu imeneyi. Kunena kuti anali maganizo chabe a Mulungu kuti tsiku lina Yesu adzabadwa padziko lapansi. *“...Pakuti munga osinkha mkati mwache, ali(nso) wotere,”* (Miyambo 23:7), ndipo munga Mulungu aganiza, Iyenso amaganiza. Mwaichi, Mau a Mulungu kapena tinene kuti maganizidwe ake ndiye Mulunguyo: *“Mau ndiwo Mulungu”*. Chifukwa chaichi, pali kulumikizana kwakulu pakati pa Mulungu ndi Mau ake: kufanana munga pa Masalmo 29:8 anenera: *“Liwu la Yehova ligwedeza chipululu, Yehova agwedeza chipululu cha Kadase.”* Ngakhale mfundo munga; *“Koma simundimvera Ine ati Yehova”* (Yeremiya 25:7) sizachilendo m' mabuku a

aneneri ngati kuti mauwa ankalankhula ndi aneneriwo. Apa Mulungu atanthauza kuti ‘simunamvere Mau anga amene ndinalankhula kudzera mwa aneneri anga’. Davide anafotokoza kuti Mau a Mulungu ndiwo nyali ndi kuwala (Masalmo 119:105), ngakhale pena ananenanso, **“Pakuti Inu ndinu nyali yanga, Yehova, ndipo Yehova adzaunika (nawala) mdima mwanga”** (2 Samueli 22:29), kuwonetseratu kufanana pakati pa Mulungu ndi Mau ake. Tikhoza kumvetsa kotero, kuti Mau a Mulungu akukambidwa ngati kuti ndi Mulungu amene. Apa tionanso kuti Mau a Mulungu amakambidwa ngati kuti ndiwo Mwini ngakhale sali choncho (onani Mpatuko wa Chisanu pamene tafotokoza za mau onena za umunthu).

Mulungu ndiye choonadicho (Yohane 3:33; 8:26; 1 Yohane 5:10), choncho, Mau a Mulungu ndicho choonadicho (Yohane 17:17). Chomwechonso, Yesu akudzitchulanso choonandi mogwirizana ndi Mau akewo; **“Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mau anga, ndi kusawasunga, ali naye womuweruza iye; mau amene ndalankhula, iwowa adzamuweruza tsiku lomaliza** (Yohane 12:48). Yesu alankhula za mau ake ngati kuti ndiwo munthu weni weni mwachitsanzo, ngati kuti ndiwo Iye weni weni. Mau ake apa akambidwa ngati kuti ndiwo munthu chifukwa afanana ndi zolinga za Khristu’yo.

Mau a Mulungu akambidwanso ngati kuti ndiwo munthu, tione chitsanzo ichi; Mulungu ngati Iye Mwini m’mau akewo (Yohane 1:1-3). Mwaichi, tiwerenga za Mau a Mulungu kuti; **“Zonse zinalengedwa ndi Iye”** (Yohane 1:3). Koma **“Mulungu analenga”** zinthu zonse mwa lamulo la Mau ake (Genesis 1:1). Chifukwa chaichi, Mau a Mulungu amakambidwa ngati mauwo ndi Mulungu weni weniyo. M’chikhristu ndi chikhulupiriro chathu, tiyenera kuzindikiranso kuti mwa mphamvu ya Mau a Mulungu mwaife, tingayandikire chifupi ndi Mulunguyo.

Zikuwonekeratu kuti Mulungu mu Genesis 1 analenga zonse mwalamulo la Mau ake osati mwa Khristu kapena ndi Yesu ayi. Anali Mau ake a Yehova amene akambidwa kuti analenga zonse osati Khristu ayi (Yohane 1:1-3). **“Zakumwamba zinalengedwa ndi Mau a Yehova; Ndipo ndi mpweya wa mkamwa mwake, khamu lawo lonse** (mwachitsanzo, nyenyezi ndi zina zotero)...**ananena ndipo chinachitidwa; analamulira ndipo chinakhazikika”** (Masalmo 33:6,9). Ndipo angakhale lero lino, zonse zochitika padziko lonse lapansi zimachitika mwa Mau ake, **“Atumiza lamulo lake kudziko lapansi;**

Mau ake athamanga mwaliwiro. Apatsa chipale chofewa ngati ubweya; Awaza chisanu ngati thonje, Aponya matalala ake ngati zidutsu; Adzaima ndani pakuzizira kwache? Atumiza Mau ake nazisungunula; Awombetsa mphepo yake, ayenda madzi ake” (Masalmo 147:15-18).

Liwu la Mulungu inali mphamvu ya chilengedwe, ligwiritsidwa ntchito pamene Yesu anapatsidwa mwa Maria. Mau a Mulungu amene awonetsanso cholinga chake, achita m’Mphamvu ya Mzimu Oyera (Luka 1:35) kotero Khristu, anabadwa mu Mphamvu imeneyi. Ndipo Maria pozindikira ichi, sanawiringule koma kunena kuti ***“kukhale kwaine monga mwa mau anu”*** (Luka 1:38).

Tawona tsopano kuti Mau a Mulungu kapena tinene kuti Mzimu /Mphamvu yake awonetsa cholinga ndi maganizo ake, ndipo kuti izi zikuwonekeratu m’Chipangano Chakale. Tikhoza kuonanso izi pa Machitidwe 13:27, pomwe tiwerenga kuti Yesu afananadi ndipo anakwaniritisa zonse zolembedwa ndi aneneri m’Chipangano Chakale: ***“Pakuti iwo (a Yuda) akukhala m’Yerusalemu, ndi akulu awo, popeza sanamzindikira Iye ngakhale Mau a aneneri owerengedwa masabata onse...”***. Khristu atabadwa Mphamvu zonse ndi Mau onse a Mulungu zinaonetsedwa mwa Yesu Khristu’yo. Yohane, motsogozedwa ndi Mzimu Oyera powuziridwa mpweya wa Mphamvuwo, analalika nalongosola za Uthenga Wabwino wa cholinga cha Mulungu ndi moyo wosatha kwaife anthu apadziko kuti zikutsamira pa Yesu Khristu amene anaonedwa ndi akuphunzira ake nagwirana nawo dzanja. Iwo pogwirana ndi Yesu, anazindikira kuti akugwirana ndi chikwaniritso cha Mau a Mulungu chimenenso chinali chikwaniritso cha cholinga cha chipulumutso mwa Khristuyo (Yohane 1:1-3). Ngakhale ife lero sitikumuna Khristu, tiyenera tisangalale pozindikira kuti tiri ndi mwayi wogawana nawo mphatso ya mtengo wapatali ya moyo wosatha pomudziwitsitsa Iye; Ndipo potero, timdziwanso Mulungu mwachindunji – komanso kuti tizindikiritsidwa za cholinga chake cha moyo wosatha umene ife tidzatsimikizidwa kuwulandira (1 Petro 1:8,9). Tiyeni tsopano tidzifunse; ‘Kodi ine ndimudziwitsitsa Khristu?’ Kungobvomereza chabe kuti Yesu analipodi sikutipindulira kanthu kena kalikonse. Tiyenera kumudziwitsitsa Iye powerenga Baibulo mozama komanso mosalekeza ndinso kupemphera mchoonadi chake ndi mtima wathu wonse modzikhuthula, ndipo tikatero, tidzamuzindikira. Ifenso tikatero, tidzapanga

ubale wamphamvu ndi Khristuyo. Mnjira imeneyi, tidzalola Iye akhale mwaife pobatizidwa mu ubatizo weni weni mwa Khristu'yo.

Mau apadera: “Pachiyambi panali mau” zipereka ndemanga yamphamvu komanso yomveka bwino ya a Yuda kuti anali khulupirira pa zolembedwa m'mabuku asanu oyamba m'Chipangano Chakale, kuti '*Mau*' analipodi kale chilengedwe chisanachitike ndi Mulungu. Yohane 1:1-3 akuwonetsa kuti tiyenera tidziwe 'mau' amenewa kuti ndiwo ulosi umene unayenera kulozera zakubwera kwa Khristu Yesu; Mulungu adali ndi cholinga m'maganizo ake chilengedwecho chisanachitike (cp. Luka 1:70).

MPATUKO 22: 'YESU KHRISTU POONA MBIRI YAKALE'

Ena amanena kuti Yesu sanayambe wakhalapo padziko lapansi lino ndipo mwaichi, chikhristu nchabodza chifukwa chimatsamira pa chikhulupiriro chosayenera komanso pa bodza la anthu popeza anthuwo anapeka nkhani ya Khristu namalalikira za Khristu wa Nazaretiyo. Iwo amapitirira ponenanso kuti anthu ambiri akhala akukhulupirira nkhani yabodza yotere yonena za Khristuyi kwa zaka pafupi fupi 2,000 zapitazo mpaka ena akumalolera kuphedwa chifukwa cha dzina la Khristuyo ngakhale kuti ndi chikhulupiriro chabodza. A Yuda ndi akhristu samaona bvuto kumva kuti kudziko kuno kudaali Muhamadi ndipo amamvetsa nagwirizana nawo iwo amene amakhulupirira kuti Muhamadi analipo padziko lapansi ngakhale kuti samagwirizana nazo zimene okhulupirira Muhamadiwo amalalikira. Ife tidziwanso kuti pali anthu ambiri amene adalipo omwe anatchukanso m'mbiri ya dziko lapansi chifukwa cha gawo lawo limene anachita akadali ndi moyo ndipo sitingafune umboni wina wapadera za iwo ayi. Iwo onse adalipo ndipo anachitadi zosiyana siyana pa mbiri ya mayiko awo.

Ngakhale ena samafuna kulola kuti Yesu Khristu adalipo padziko lapansi lino, ife akhristu monga timawerenga, tiyenera kuzindikira kuti ngati iwo safuna kubvomereza za Khristu kuti ndi Mesiya, kapena tinene kuti Mpulumutsi, kuyenera kukhala kobvuta kuti iwo pawokha aloledi mphamvu za Yesu Khristu. A Yuda anamudziwadi Yesu Khristu chifukwa anamuona

m'chirumika choyambacho. A Gary Habermas, amene anaphunzira kwambiri pa mbiri ya kale, akutitsimikizira kuti 'Yesu Khristu wa ku Nazareti' analipodi. Tikawerenga chibuku chawo chotchedwa "Ancient Evidence For The Life of Jesus", tizindikira ndi kutsimikizira izi mopanda chikayiko.

A Tacitus anali m'Roma amene ankawerenga kwambiri ndi kulemba Mbiri Yakale ndipo m'mabuku awo otchuka awiri, omwe anatchedwa "Annals" ndi "Histories" onse, anakambapo za Yesu ndi chikhristu mzaka za AD115 ngakhale kuti iwo sanali mkhristu. Iwo analemba motere m'mabuku amenewa:

"Kagulu ka anthu kotchedwa akhristu kamene kanadedwa ndi anthu ena ambiri, kamenenso dzina lawo linachokera mliwu loti '*christus*' anazunzidwa, nanyozedwa mnthawi ya ulamuliro wa Tiberius pamaso pa m'modzi wa wachiweruzo chamalamulo amene ankatchedwa '*Pontius Pilate*'".

Udindo wa Tiberius udalipo mzaka za 14 mpaka 37 AD, nthawi imene Yesu Khristu adaphedwa malingana ndi mabuku amenewa. A Tacitus anafotokozanso mmene iwo amaonera kuti chipembedzo ndi chikhulupiriro chimenechi ndi gulu lawo "chinayambira ku Yudeya ndinso kufalikira kwambiri mpaka ku Rome", koteronso, akupitiriza m'mene anthu ena sanakondwere ndi akhristu ndipo kuti ambiri mwa akhristu'wo anaphedwa ku Rome. Zonsezi tiona kuti zikugwirizana komanso kulumikizana bwino ndi zimene timawerenga m'Buku Lopatulika m'Chipangano Chatsopano ponena za Yesu Khristu, omutsatira ndinso ophunzira ake, kufalikira kwa Uthenga Wabwino kuchokera ku Yudeya, kenaka mdera lonse la Ufumu wa a Roma mpaka ku Rome kumene. Ndipo akufotokozerana m'mene onse otsatira Yesu anawazunzira ngakhale kuwapha chifukwa cha chikhulupiriro chawo cha Uthenga Wabwino wopezeka m'Buku Lopatulika wonena za Yesu Khristu.

A Suetonius, mmodzi wa nzika za ku Rome amenenso ndi odziwika bwino lomwe m'mbiri zakale, anakambapo za ulamuliro wa '*Claudius*' mfumu ya a Roma (mzaka za 41 mpaka 54AD): kuti "*Chifukwa cha zipolowi zimene zinabwera ndi a Yuda, Claudius anathamangitsa a Yuda onse mu mzinda wa Rome*". Dziwani kuti "*Chrestus*" ndi malembedwe ena a dzina loti '*Christ*' limene M'Chichewa timati *Khristu*. Moteronso, Machitidwe 18:2 akufotokozerana m'mene banja la Acquilla ndi Priscilla anathamangitsidwira kuchoka ku Rome chifukwa cha nkhanza zimene akhristu ndi a Yuda

analandira ponyozedwa, kuzunzidwa ndi kumenyedwa. A Suetonius akuthirira ndemanga yawo pa kuzunzidwa kwa a Yuda m'nthawi ya Nero: ***“Pamene moto waukulu unawoneka mu mzinda wa Rome, ...kunali mzunzo ndi chilango chachikulu kwa akhristu onse, kagulu kamene kanayambitsa chikhulupiriro ndi chipembedzo chachilendo”*** Apa tiona kuti Khristu analipodi ndipo kuti adali ndi omutsatira ake ambiri m'chirumika chimenechi.

A FF Bruce (mbuku lawo ***“Christian Origins”***) akupereka chithunzi cheni cheni cha mbiri yakale yokhudza ku m'mawa kwa nyanja ya Mediterranean mogwirizana ndi wolemba wina wotchedwa ***Thallus*** mzaka za 52AD. A Bruce akutiwonetsa (mbuku lawo lina lotchedwa ***“The New Testament Documents”, pa tsamba 113***) kuti ophunzira wina wambiri yakale wotchedwa ***Julius Africanus*** anakambapo za zimene a ***Thallus*** analemba monyozera ponena za mdima umene unagwa pamene Khristu anapachikidwa pa mtanda, nanena kuti izi zinachitika chifukwa cha kukumana kwa mwezi ndi dzuwa. Izi zikuonetsanso kuti a ***Thallus*** analembapo kale za mbiri ya kupachikidwa kwa Yesu pamtanda kumbuyo kwa chaka cha 52AD.

A Pliny amene ankagwira ntchito m'boma la chi Roma panthawiyo, akunena motsimikizira ndithu kuti kunali kagulu ka anthu kotchedwa akhristu mzaka zomalizira za mchirumika choyamba. Iwo anaona kuti akhristu ankasunga pangano lawo lokumbukira Yesu Khristu m'njira yapadera nthawi zonse ponyema mkate ndipo pa ichi akupereka ndemanga iyi: ***“Iwo ankayetsa kukumana pa tsiku limene iwo adayika padera kuti azikumbukira Khristu mwapadera poyimba nyimbo zake ndi kumutamanda”*** (Letters of Pliny,” translated by W. Melmoth, Vol.2, X:96). Mafumu a chi Roma – ***Trajan*** ndi ***Hadrian*** onse anakambapo za bvuto limene iwo ngati mafumu, ankalipeza pofuna kulongosola nkhani zokhudza akhristu. Mukhoza kuwona izi m'buku lotchedwa “ ***‘Letters of Pliny,’*** Vol.2, X:97 ndinso mabuku a ***‘Eusebius Ecclesiastical History, IV:IX’*** ”. Zonsezi zikutitsimikizira ndi kuonetsera poyera kuti kagulu kameneka kankatsatira Khristu weni weni wamoyo amene analidi pakati pawo m'nthawi imeneyi mchirumika choyambacho.

‘Talmud’ buku loyera la chi Yuda mu Sanhedrin 43a, likulongosola bwino zaimfa ya Khristu Yesu. Buku limeneli linadziwika bwino kuti linalembedwa mzaka za 70 mpaka 200AD: ***“Pa nthawi ya ‘Paskha Yeshu* (Yesu) ***anapachikidwa. Kwa zaka 40 asanapachikidwe, kunalalikidwa kuti*****

adzalasidwa ndi miyala chifukwa anawukira, nakopa ana a Isreali akane chipembedzo chosayeneracho. Yense wakunena zabwino za Iye, abwere nazunzika mmalo mwa Iye'. Ndipo popeza sanamfunire zabwino, Iye anapachikidwa pamtanda patsiku la Paskha". Kupachikidwa kwa Yesu ndiko kukhomedwa pamtanda kwa Yesu Khristu (Agalatiya 3:13; Luka 23:39). Ndime zimenezi zikunena mmene a Yuda anafunitsitsira kuti aphe Yesu zomwe zinagwirizana ndi chilamulo cha Mose ndipo komalizira, Yesu Khristu anaphedwadi. Izi zinachitikadi pogwiritsa ntchito Malamulo a chi Roma.

'*Sanhedrin 43a*' akufotokozeranso m'mene akuphunzira asanu a Yesu anaweruzidwira naphedwa, kuonetsadi kuti a Yuda anaonadi, nakhulupirira Yesu Khristu m'mbiri imeneyi. '*Sanhedrin 106b*' akufotokozeranso motsimikizira kuti Yesu adali ndi zaka 33 pamene adamwalira, ndipo kuti izi zikugwirizana ndi zimene zinalembedwa m'Chipangano Chatsopano. '*Maier*' ("First Easter," *pg.117,118*), akunenapo za buku lotchedwa "*Toledoth Jesu*", limene lidakambapo zonama ponena kuti akuphunzira a Yesu anayesetsa kukaba thupi la Yesulo atamwalira, ndipo ogwira ntchito ya ulonda kumandako amene ankatchedwa Yuda atamva, anakawulula nachenjeza kuti akachotse thupi la Yesulo limene kenaka analipereka kwa a Yuda. *Justin Martyr* polemba mchaka cha 150AD anatumiza uthenga kuti thupi la Yesu Khristu linabedwa ('*Dialogue with Trypho,*' 108) ndipo *Tertilian* ('*On Spectacles,30*') analembanso motsindika nkhani yomweyi mzaka za 200AD. Tikaonetsetsa zinthu zonsezi, tiona kuti a Yuda a nthawi imeneyo anakhulupirira ndipo anali odziwa bwino nkhani yakuti Yesu anabvutika koposa mpaka kufa imfa yowawa yochititsa manyazi ngakhale adali munthu wodziwika bwino pakati pawo.

Wolembe wina wa chi Greek mchirimika choyamba wotchedwa *Lucian*, analemba monyodola akhristu amene '*amapemphera munthu wophedwa mpaka lero*', ("Lucian, The Death of Peregrine, 11-13", in 'The Works of Lucian', Vol.4, translated by Fowler and Fowler).

Josephus ndi mmodzi mwa anthu olemba mbiri yakale mchirimika choyamba ndipo mbuku lake lotchedwa "*Antiquities*", mzaka za 90-95AD, akunena za Yakobo (James) m'bale wake wa Yesu, amene anatchedwa Khristu. Akunenanso m'buku lomweri za Chipangano Chatsopano pofotokozeranso za chithunzi thunzi cha Yesu kuti: "*Tsopano panali nthawiyi Yesu, munthu*

wanzeru zoposa, amene ananena zozizwitsa, Iye anali Khristu....amenenso anawonekera kwa omutsatira ake ali wamoyo patatha masiku awiri atafa, tsiku lachitatu atafa kale,...monga aneneri ambiri analosa za Iye mazana mazana a zinthu zodabwitsa zimene Iyeyo anachita...”.

Anthu ambiri anayikapo ndemanga pankhani imene Josephus analemba pokhudza Yesu wa ku Nazareti amene anakhala mzaka za chirumika choyambacho. Ndipo zina mwa ndemangazo zinali motere:

- *Eusebius* (Ecclesiastical History, 1:XI) anayikapo maganizo ake pa mfundo imeneyi yosimba za Yesu imene Josephus analemba.
- *Ophunzira apamwamba a ukachenjede* ambiri anayamikira koposa ntchito yabwino yaikulu ya Josephus pankhani ya Yesu Khristu (*onaninso “Daniel Rops, ‘The Silence of Jesus’ Contemporaries,”* pg.21; J.N.D. Anderson, *“Christianity: The Witness of History* pg.20; *F.F. Bruce, “The New Testament Documents” PG.108,109*).
- Palibe umboni owonetsa kuti zolembedwazo zinangolembedwa mwamaganizo a munthu ayi .
- Ndipo Professor Schlomo Pines ananena kuti buku loyambirira lolembedwa m’chi Arabia la Josephus linapezeka ndipo kuti ndime zalembedwa pamwambazi ziripodi m’buku limeneri limenenso silikukambapo kanthu kena kalikonse kokhudza chi khristu ngakhale kuti zimene zidalembedwazo zikufanana ndi zomwe zidalembedwadi m’Baibulo. Tionanso kuti ngakhale Josephus adali m’Yuda, iye ngati wolembe za mbiri yakale osati olembe Baibulo, sanayikepo maganizo ake kapena chikhulupiriro chake za Mesiya kapena kuukanso kwa akufa kwa Yesu ayi. Pines analengezeratu zonse zimene iye anazipeza mkufufuza kwake mu *“The New York Times” February, 12 1972*, momwenso akuyika maganizo a Josephus pokhudza Yesu Khristu mzimene zinalembedwa m’chi Arabia: *‘Panthawi imeneyi, kunali munthu wanzeru zoposa amene adadziwika ndi dzina loti “Yesu”. Ndipo makhalidwe ake anali abwino, odzichepetsa komanso waulemerero. Motero, anthu ambiri kuphatikizapo a Yuda ndi anthu a m’mayiko ena anamutsata Iye namukhulupirira. Pilato anamunyoza, nalamula kuti Yesu apachikidwe pamtanda naafa. Ndipo ena onse omutsata aja sanamutaye koma anamutsatabe. Kenaka omutsatawo ananena za Yesu. Iye anaonekera kwa iwo patatha masiku atatu; ndipo kuti anakhalanso moyo kotero, anatsimikizira kuti anali Mesiya amene aneneri ankalosera.”* Nkhani imeneyi ikugwirizana kwathunthu ndi zonse zimene zidalembedwa m’Chipangano Chatsopano zonena za Yesu Khristu wamoyo.

MPATUKO 23: PAKUTI NDINATSIKA KUMWAMBA

“Pakuti mkate wa Mulungu ndiye wakutsika kuchokera kumwamba ndi kupatsa moyo kwa dziko lapansi.....Pakuti ndinatsika Kumwamba” (Yohane 6:33,38).

Mau amenewa ndi ena ofanana ndi amenenso sakugwiritsidwa ntchito moyenera mmatcharitchi ambiri, ndipo amalepheradi kuthandiza maganizo osokera mmatcharitchimo pamene anena kuti Yesu Khristu adalipo kale kumwamba Yesuyo asanabadwe. Tiyeni tionere limodzi mfundo zotsatirazi kotero, tiziganizira ngati chikhulupiriro choterechi nchoonadi pakati pathu mofaniza zimene timawerenga m’Baibulo:

1. Alaliki a milungu itatu mwa mmodziyo amanena zinthu zimenezi pofuna kutsimikizira mfundo zawo kuti ndiyo yoona. Koma tikakhulupirira zimenezi, sitingathe kuonetsa umboni wa mfundo imeneyi wochokera m’Baibulo. Zikomo kuti tikudziwa kuti Yesu anabadwa kuchokera mchiberekero cha Maria. Sitifuna titsutsane ndi Baibulo kotero, pokhulupirira zimene alaliki ena amalalikira zimene sizipezeka penapaliponse m’Buku Lopatulika. Yohane 6:60 tiwerengapo za mau ***“osautsa kuwamva”*** kotero, tiyeni tonse tizimvetsa bwino tisanakhulupirire zimene tawuzidwa.
2. Pa Yohane 6, Yesu akufotokozapo za kufanana pakati pa Iye ndi manna. Manna anatumizidwa ndi Mulungu mnjira yoti Mulungu anapanga chakudyachi ngati chizindikiro cha Yesu kwa anthu adziko lapansi. Manna sadalipo kalelo mpaka pamene Mulungu anawapanga nawapereka kwa ana a Israeli. Moteronso, Yesu anabadwa mwa munthu monga munthu anabadwa mwamkazi. Yesu Khristu anabadwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera umene unakuta Maria, nakhala ndi pathupi (Luka 1:35).
3. Yesu akunena kuti ***“...Mkate umene ndidzapatsa Ine, ndiwo thupi langa*** (Yohane 6:51). Thupi la Yesu kotero, silinali Mulungu monga ena akunenera ayi, koma thupi leni leni monga lathuli osati lochokera kumwamba ayi. Nchifukwa chake, Yesu akunena kuti ***“thupi”*** lakelo liri ngati mkate (manna) lochokera kumwamba (chifukwa Yehova ndiye anapereka). Kotero, Yesu akufananiza mkate wochokera kumwambawo ndi thupi lakelo lomwe ndi la ***“mwana wa munthu”*** (Yohane 6:62) osati ***‘mulungu Mwana’*** ayi.

4. M'nunsu yomweyi ya Yohane 6: ndizoonekeratu kuti Yesu akupereka chithunzi thunzi chakuti sanali ofanana ndi Mulungu. *“Atate wa moyo anandituma Iye”*, (Yohane 6:57) akutsimikizira kuti Yesu ndi Mulungu sakufanana mpang'ono pomwe. Ndipo *“Inenso ndiri ndi moyo chifukwa cha Atate”* awonetseratu kuti Iye siofanana chifukwa Iye payekha sangakhale ndi moyo koma mwa Atate monga ifenso.
5. Tiyeni tsopano tifunsane kuti kodi Yesu anabwera liti pansi pano, ndipo kuti anabwera bwanji kuchokera kumwamba? Alaliki ena amati Yesu anabwera pansi pano pamene Iye anabadwa. Koma Yesu Iye Mwini amati ndiye *“mkate wa Mulungu wakutsika kuchokera kumwamba ndi kupatsa moyo kwa dziko lapansi”* (Yohane 6:33,50). Ponena za mphatso ya Mulungu imene ndi Yesu, Khristu ananena kuti *“...Atate wanga akupatsani inu mkate woona wa kumwamba”* (vs.32). Pamene Yesu ananena izi nkuti Khristu'yo atabwera kale pansi pano chifukwa zonsezi zinali kale mmaganizo mwa Mulungu kalelo. Nchifukwa chake akunena kuti *“Ine ndine mkate wamoyo womwe unatsika kuchokera kumwamba”* (vs.51). Izi akukambanso poganizira za imfa yake yodzachitika kutsogolo kwake. Motero apa, Yesu akunena ngati kuti adzabwera, wabwera ndiponso kuti anabwera kale poonanso za imfa yake pamtanda paja. Choncho, adzabwera, anali Mulungu mmaganizo mwake osati pamene Yesu anabadwa ayi; - tiwerenganso izi ngakhale m'Chipangano Chakale pamene timva za mazunzo a ana a Israeli ku Aigupto pomwenso anapulumsidwa ndi Mose. Koteru, kutumizidwa kwa Yesu kufanana ndi kutumizidwa kwa Mose. Izi choncho, ndizo zizindikiro.

MPATUKO 24: KODI KHRISTU ANALENGA DZIKO LAPANSI?

“...wobadwa woyamba wachilengedwe chonse; pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi zapadziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yachifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye. Ndipo Iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa Iye. Ndipo Iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo; ndiye chiyambi,

wobadwa woyamba woturuka mwa akufa; kuti akakhale Iye mwa zonse woyambayamba” (Akolose 1:15-18). **Iyi ndi imodzi mwandime zimene ambiri amanena kuti Khristu analenga dziko lapansi.**

1. Ngati izi ndizoona, ndiye kuti ndime zina zambiri zimene zimafotokozera kuti Yesu kunalibe kalelo asanabadwe nzabodza.. Tikawerenga m’Buku la Genesis, tiona chizindikiritso kuti Mulungu ndiye Yekhayo analenga zonse padziko lapansi ndi kumwamba. Tikhoza kuona kuti payenera kukhala Mlengi m’modzi yekha, Yesu kapena Mulungu Yehova. Ngati Mulungu ndi amene analenga Yesu Khristu koteru, ndiye kuti Mlengi Yekhayo ndi amene ali ndi mphamvu zonse za chilengedwe ndipo ndi Yehova Mulungu wathu. Nchifukwa chake, ngakhale Yesu Khristu abvomereza kuti sanalenge chirichonse koma kuti anadza kukwaniritsa cholinga cha Namalengayo pakati pa anthu.
2. Yesu anali **“wobadwa woyamba”** kutanthauza kuti anachita kuyamba, ‘chiyambi’. Palibe umboni umene ungamitsimikizire kuti Yesu analipo chilengedwe chisanachitike ayi. Titha kuonanso 2 Samueli 7:14 ndi Masalmo 89:27 ndime zimene zikutiunikira kuti Yesu Khristu amene anali Mwana wa Davide, anayenera kukhala **“Mwana woyamba wa Mulungu”**. Ndime zimenezi zinalosera chabe za kubadwa kwa Yesu chifukwa Khristu panthawiyo anali asanabadwe. Yesu anakhala **“Mwana wamwamuna wa Mulungu ndi mphamvu”** pamene anauka kwa akufa (Aroma 1:4). Mulungu **“analikwaniritsapakuukitsa Yesu; monganso mulembedwa m’Salmo lachiwiri, Iwe ndiwe Mwana wanga lero ndakubala”** (Machitidwe 13:32,33). Koteru, Yesu anasanduka **“Mwana woyamba wa Mulungu pamene anaukitsidwa kwa akufa”**. Onaninsu kuti Mwana wa Atate wokhala kudzanja lamanja afanizidwanso ndi Mwana woyamba (Genesis 48:13-16), ndipo kuti Yesu anakwezedwa nakhala kudzanja lamanja pamne anakwaniritsa cholinga cha Mulungu naukitsidwa kwa akufa (Machitidwe 2:32; A Hebr 1:3).
3. Nchifukwa chake Yesu akutchulidwa **“Mwana woyamba kuchokera kwa akufa”** (Akolose 1:18), liwu limene likufanana ndi **“wobadwa woyamba wa chilengedwe chonse”** (Akolose 1:15). Motero, Iye akamba za Iye Mwini ngati **“wobadwa (woperekedwa) woyamba wa**

akufa...chiyambi cha chilengedwe ndi Mulungu” (Chibvumbulutso 1:5; 3:14). Yesu anali woyamba wa chilengedwe cha amuna ndi akazi osafa, amoyo, opulumutsidwa, amene kuukitsidwa kwao ndi kubadwa kwathunthu ngati anthu osaona imfa kunatheka chifukwa cha imfa ndi kuukanso kwa akufa kwa Yesu Khristu (Aefeso 2:10; 4:23,24; 2 Akorinto 5:17). ***“Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira, choteronso mwa Khristu onse (okhulupirira) akhalitsidwa ndi moyo. Koma yense mdongosolo lake la iye yekha, chipatso chowundukula Khristu; pomwepo iwo a Khristu, pa kubwera kwake”*** (1 Akorinto 15:22,23). Iyi ndi mfundo yomwensho tamva kale m’Buku la Akolose 1. Yesu anali woyamba kuukitsidwa kwa akufa komanso woyamba kukhala ndi moyo wosatha. Khristu analinso woyamba wa chilengedwe powukitsidwa koteru, okhulupirira eni eni adzatsatira mapazi ake pamene Khristuyo adzabwerenso.

4. Chilengedwe chimene tawerenga m’Buku la Akolose 1 koteru, chikufotokozera za chilengedwe chatsopano osati cha m’Buku la Genesis ayi. Kudzera m’ntchito ya Yesu, ***“Zinthu zonse zinalengedwa...maufumu...maulamuliro”*** ndi zina zotero. Paulo pamenepa sakunena kuti Yesu analenga zinthu zonse natchula zinthu ngati mitsinje, mapiri, mbalame ndi zina ayi. Chilengedwe chimenechi chatsopano chikukamba za mpahtso zimene tidzalandire mu ufumu wa Mulungu. ***“Maudindo... maulamuliro”*** ndi zina zotero, zikulosera za mmene okhulupirira adzakhale ***“mafumu ndi ansembe kwa Mulungu wathundipo achita ufumu padziko”*** (Chimbulutso 5:10). Zonsezi zidzatheka chifukwa cha ntchito yabwino imene Yesu Khristu anagwira ali panso. ***“Zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye”*** (Akolose 1:16). M’Buku la Aefeso 2:6 timawerenga za okhulupirira pamene amene mwa Khristu adzakhala ***“mmalo aulemerero mmwambamwamba”***. Koteru, ndime zimenezi, zikutiphunzitsa kuti malo athu auzimu omwe tiri nawo, ndi zomwe tidzaone mtsogolomo, zidzatheka chifukwa cha Yesu Khristu. ***“Dziko lapansi ndi kumwambamwamba”*** ziyimira zinthu zonse zimene ziyenera zimasulidwe ndi mwazi wokhetsedwa pamtanda (Akolose 1:16,20), kuonetsera kuti ***“zinthu zonse...mmwambamwamba”*** zitanthauziradi okhulupirira onse amene adzakhale ndi Yesu ukatha moyo uno.

MPATUKO 25: “ASANAYAMBE KUKHALA ABRAHAMU NDIPO INE NDILIPO” (Yohane 8:58).

Mau awa anthu ena amawamva ngati kuti akutanthauzira chiphunzitso chimene chikuwatsimikizira kuti Yesu Khristu analipo kale asanabadwe mwa Maria.

1. Yesu sananenepo kuti **“Asanayambe kukhala Abrahamu, Ine ndidalipo kale”** ayi. Khristu analipo kale mmalonjezo a Yehova kotero, anali mwana wamalonjezani kwa Abrahamu ndi omutsatira ake. Tikati kuti Yesu analipo kale Abrahamu asanakhalepo, tipezeka kuti tikutsutsana ndi malonjezani amenewa amene analipo kale pakati pa Abrahamu ndi otsatira ake ndi Mulungu.
2. Mwanjira yomweyi, Yohane 8:58 ndicho muuni umene pozindikira za ukuru wa Abrahamu, a Yuda adayenera kudziwa bwino za mphamvu ndi kufunika kwa Yesu pakati pawo. Kotero, Yesu akuwakumbutsa pa ndime imeneyi kuti Iye anali wofunika kwambiri pakati pawo kuposa Abrahamu. Momwenso, a Yuda aja anakumbutsidwa kuti anayeneradi kulemekeza Yesu Khristu chifukwa chakuti Mulungu anayamba kukonza kale chikonzero cha chipulumutso kudzera mwa Iye Yesu pachiyambi Abrahamu asanabadwe. Koterodi, Yesu anali woyamba pakufunikira pa chipulumutso chathu Abrahamuyo asanakhalepo.
3. Titsimikizira zimenezi pamene tiwerenga Yohane 8:56: **“Atate wanu Abrahamu anakondwera kuona tsiku langa; ndipo anaona, nasangalala”** Tsiku lokhalo limene Abrahamu anaseka nakondwera ndilo tsiku lomwe iye analonjezedwa kuti adzakhala ndi mwana; iye anamvetsa kuti lonjezo limeneri linkaloseranso kudza kwa Khristu Yesu (Genesis 17:17). Abrahamu **“anaona”** kutsogolo kwa pamene malonjezani akubwera kwa Khristu anawululika kapena tinene kuti adzaululike. Nchifukwa chake adachita ndemanga yake pa kudzipereka kwa Yesu Khristu kutsogolo kwake, **“M’phiri la Ambuye, chidzaoneka”**. Ndichifukwa cha ndemanga imeneyi yomwe Yesu Khristu akutitsimikizira kuti ngakhale Abrahamu asanabadwe, Iye Khristu, anaonedwa kale m’masomphenya a Abrahamu. Yesu kotero,

anamvetsa kuti malonjezano amene Yehova anapangana ndi Abrahamu ankalosera za Iye ndipo Abrahamu anachitira umboni nadziwanso za chimenechi. Takamba kale mgawo 3.1 kuti malonjezano a Mulungu kwa Abrahamu, anafotokoza za cholinga cha Mulungu pokhudzana ndi mbiri ya Yesu ndipo kuti chikonzero chimenechi Mulungu anali atakonza kale kuchokera pachiyambi. Cholinga chimenechi motero, chinaululidwanso kwa Abrahamu ndipo tsopano chinkakwaniritsidwa pakati pawo a Yuda aja. Kotero, **“Mau (malonjezano) *anasanduka mnofu*”**.

4. Ena amanena kuti Yesu pa ndime imeneyi ankamba za dzina la uMulungu pogwiritsa ntchito liwu loti **“Ndine”**. Tafotokoza kale mgawo 3 kuti Yesu komanso anthu wamba ena onse akhala akutchulidwa mu uMulungu angakhale kuti iwo sindiwo Mulungu. Tikhulupirira kuti Yesu anachita chimodzimodzi podziwa kuti anthu nthawi imeneyo ankamumvetsetsa chimene ankanena ngakhale kuti anthu lero amapotoza dala mfundo zotere ncholinga chakuti akwaniritse zolinga zawo. Tikawerenga Yohane 9:9 tiona kuti munthu wakhungu uja atachira, ena mwa anthu amene anaona izi anayamba kunena kuti sanali iye amene anali wakhungu ayi koma kuti adafanana naye chabe. Koma ena mwaiwo anakhulupirirabe nanena kuti ndi iye basi. Liwu loti ‘iye’ mchilankhulo cha chi Greek linamasuliridwa ngati kuti **“NDINE”** lomwe likupezekanso pa ndime imeneyi-Yohane 8:58. Kotero, liwu loti **“Ndine”** silikuyimira Mulungu monga Yesu wagwiritsira ntchito chifukwa ngakhale munthu ponena za munthu wakhungu uja anagwiritsanso ntchito liwu lomwelo mchi Greek. Choncho liwuli sindilo **“INE NDINE YEMWE NDIRI”** wa pa Eksodo 3:14 ayi koma **“Ndine”** basi.

MPATUKO 26: MELIKIZEDEKE

Ambiri mwa anthu amene amawerenga Baibulo amayamikira kwambiri akamva malembo a Petro pamene azindikiritsa kuti **“...Monganso m’bale wathu Paulo, monga mwa nzeru zopatsidwa kwaine, anakulemberani; monganso mmakalata ake onse muli zobvuta kuzizindikira, zimene anthu osaphunzira ndi osakhazikika apotoza, monganso ateronawo malembo ena, ndi kudziononganso nawo eni”**, (2 Petro 3:15,16). Ndime imeneyi

ikhoza kutiunikiranso kuti amodzi mwa mau obvutawa m’Baibulo, ndiwo kamvedwe ka nkhani yonena za Melikizedeke yomwe yalembedwa m’Buku la A Hebri 5:10,11,14 yomwedi ndi anthu ochepa okha amene amatha kuyimvetsa bwino ndinso kuyimasulira moyenera.

“Pakuti Melikizedeke uyu, Mfumu ya Salemu, Wansembe wa Mulungu Wamkulukulu, amene anakomana ndi Abrahamu, pobwera iye adawapha mafumu aja, namdalitsa” akukambidwa kuti ***“...wopanda atate wake, wopanda amake, wopanda mawerengedwe a chibadidwe chake, alibe chiyambi cha masiku ake kapena chitsiriziro cha moyo wake, wofanizidwa ndi Mwana wa Mulungu...”*** (AHebri 7:1-3). Ena amatengera ndime imeneyi pofuna kutsimikizira kuti Yesu adalipo kale asanabadwe mwa Maria.

Yesu anali ndi Atate wake (ndiye Mulungu) ndi amai ake (ndiye Maria) ndipo timawerenga za tsinde lake la Yesu Khristu pa Mateyu 1, Luka 3; komanso Yohane 7:27. Nkhani ya Melikizedeke choncho, sikunena za Yesu ngati munthu ayi. Dziwaninso kuti Melikizedeke anangofanizidwa ngati ***“Mwana wa Mulungu”*** (AHebri 7:3); kotero, sanali Yesu ayi koma adali ndi zifanifani za Yesu Khristu zimene zingagwiritsidwe ntchito pa maulaliki athu. ***“..Kwadziwikatu koposa kuti auka Wansembe wina monga mwa mafanizidwe a Melikizedeke,”*** (AHebri 5:5,6).

Zimene zalembedwa m’Buku la AHebri ndi ziphiphiritso. Ngati Melikizedeke analidi munthu weni weni, wopanda atate wake wopanda mai ake; ndiye kuti iye anali Mulungu; Yehova ndi yekhayo amene alibe chiyambi (1 Timoteo: 6:16; Masalmo 90:2). Koma akusyanabe ndi Mulungu monga tikuwerenga pa AHebri 7:4; ***“Koma tapenyani ukuru wake wa iyeyu...”*** komanso onani kuti iye anaonedwa ndi anthu wamba, Mulungu satero ayi, palibe munthu amene anaona Mulungu; iyeyu ankapereka nsembe kwa Mulungu, Yehova ndiye amalandira nsembe zathu. Ngati atchulidwa munthu, ayeneranso kotero, kuti adali ndi makolo ake. Mwaichi, ***“wopanda amake, wopanda tsinse lake”*** zikhozanso kutanthauzira kuti mbiri ya makolo ake siyinadziwike bwino m’Baibulo kapenanso kuti siyinali yofunika panthawi imeneyi. Mwachitsanzo, makolo a Estere nawo sanalembedwe m’Buku Lopatulikandipo moteronso Estere akufotokozedwa ngati kuti sanabadwe mwa makolo ena aliwonse.

“Ndipo iye adalera Hadasa, ndiye Estere, mwana wamkazi wa atate wake wamng’ono; popeza iye analibe atate kapena amai; ndi namwaliyo anali wamaonekedwe okoma, ndi wokongola; ndipo atamwalira atate wake ndi mai wake, Moredekai anamtenga akhale mwana wake” (Estere 2:7).

Buku la Genesis kawiri kawiri limafotokozera bwino zonse za mbiri ya tsinde la munthu m’Buku Lopatulika. Koma tiwona kuti nkhani ya Melikizedeke sinafotokozedwe mwamtundu wotere monga mmene zinthu zirili mnkhani zinazo. Makolo ake ndi tsinde lake zonse sizinatchulidwe mnkhani imeneyi. Tikhoza kuona kuti Melikizedeke anali munthu wofunikira kwambiri pa mbiri chipulumutso. Iye anali wamkulu zedi ndipo nzodziwikiratu kuti anachita zinthu zazikulu koma sitikuwerenga zambiri zaizi ngakhale kuti adali munthu wolemekezeka chomwechi. Abrahamu naye anapereka ulemu ndi chiwongo kwaiye ndipo Abrahamu analandiranso madalitso kuchokera kwa Melikizedekeyo kuonetsadi kuti anali munthu wamkulu kwaiye (AHebri 7:2,7).

Paulo sakunena nkambakamwa chabe ayi. Panali bvuto lalikulu zedi limene nkhani ya Melikizedeke inabweretsa pakati pa a Yuda nthawi imeneyo. A Yuda mwina ankafunsa: *“Akhristu inu mukutiiza kuti Yesu wanuyu ndiye wansembe wathu wamkulu, amene angatiwunikire ndikutithandiza mkupemphera komanso kutiunikira njira ya Mulungu Atate. Koma ife timadziwa wansembe ayenera kukhala munthu amnene ndiwodziwika ndipo kuti ali ndi tsinde la Levi . Tidziwa kuti inu mukhoza kunena kuti Yesu anali wa mfuko la Yuda (AHebri 7:14). Koma ife tikudziwa kuti Abrahamu ndicho chitsanzo cha chipembedzo chathu koteru, Yesu wanuyu sitikumudziwa”* (Yohane 8:33,39).

Paulo akuyankha mndime zimenezi kuti: ‘Kumbukirani kuti Melikizedeke analibe tsinde lina lirilonse koam ngakhale Abrahamu anazindikira ukulu wake pamaso pa Mulungu chifukwa anali mfumu komanso wansembe. Mpulumutsinso ayenera kukhala Wansembe komanso Mfumu monga mwa dongosolo la ufumu ndi unsembe wake wa Melikizedeke (AHebri 5:6 cp. Masalmo 110:4). Mwaichi, Abrahamu anali wamng’ono koteronso, dziwani kuti Yesu posayang’ana zinthu zosafunikira ngati tsinde la munthu pakati pathu, alinso Wamkulukulu (1 Timoteo 1:4). Mukaganiza mofatsa nimulumikiza bwino mfundo imeneyi, mudzatha kuona kuti ulosi wa

Melikizedeke unayandikira kwambiri pa ntchito yaikulu imene Yesu anagwira ndipo nayikwaniritsa pakati pathu.
Nkhani imeneyi lero ndiyo phunziro lathu kuti pakati pathu akhoza kupezekapo a Melikizedeke ambiri.

PHUNZIRO 7: MAFUNSO

1. Nenani maulosi awiri a mChipangano Chakale amene adanenera za Yesu
2. Kodi Yesu adalipo mu uthunthu wake Iye asanabadwe mwa Maria?
3. Kodi Yesu adakhalapo mwanjira yanji Iye asanabadwe mwa Maria mayi wake?
 - (a) Monga mngelo
 - (b) Ngati Mulungu mmodzi mwa atatuwo
 - © Mwa Mzimu
 - (d) Mmaganizo ndi Mcholinga cha Mulungu basi
4. Ndi ziganizo ziti mwa ziganizo zotsatirazi zomwe ziri zowona ponena za Maria?
 - (a) Anali mzimayi wabwino, komanso wosachimwa
 - (b) Adali mzimayi wamba
 - (c) Anakhala ndi pakati mwa Mphamvu ya Mzimu Woyera
 - (d) Pakadali pano amatipempherera kudzera mwa Yesu Khristu
 - (e) Adali buthu losachimwa lopanda banga
 - (f) Sanadziwe mwamuna mpaka atakwatirana ndi Yosefe
 - (g) Anali wochimwa pachibadidwe
5. Kodi Yesu analenga nawo dziko lapansi? Perekani chitsanzo cha umboni wanu pankhaniyi?
6. Kodi inu mumamva bwanji mukawerenga Yohane 1:1-3? *“...Pachiyambi panali mawu.”* Nanga izi sizitanthauzanji mkamvetsedwe kanu?
7. Chifukwa chiyani inu mumakhulupirira kuti Yesu sadalipo Iye asanabadwe mthupi kalelo?

Mukayankha mafunso'wa chonde tumizani ku imodzi mwa ma adiresi mwapatsidwa m'mapeji oyambirira a buku lino.

PHUNZIRO 8

UTHUNTHU WA YESU

8.1 UTHUNTHU WA YESU – MWACHIDZIWITSO

Nchoopsa kwambiri mchikhristu chathu kuwona kuti Yesu Khristu lero, sakulandira ulemu woyenera komanso kuti anthu lero tikulephera kukweza ndi kutamanda dzina lake poona kuti Iye ndi amene anagonjetsa tchimo, natukula miyoyo yathu mu uzimu. Angakhale anthu amene akhulupirira za Mulungu mmodzi mwa atatuwo amuyesadi Iye mmodzi mwa milungu itatuyo. Popeza Mulungu sangayesedwe (Yakobo 1:13) ndipo kuti nzosatheka kuti angachimwe (nanga achimwira ndani?), apa zingaonetse kuti Yesu sanayenera kulimbana ndi tchimo. Umoyo wake kotero, unanyozeka, nakhala monga munthu wina aliyense amakhalira padziko lapansi ngakhale Iye za mdziko adalibe nazo gawo.

Tionanso gawo lina kuti magulu ena ngati a mboni za Yehova ndi a chikhulupiriro cha ‘mormon’ samatha kuzindikira bwino nakhutitsidwa pa chodabwitsa cha Yesu Khristu amene ali Mwana Yekhayo Wobadwa Yekha wa Mulungu. Mwaichi, sizingatheke kuti tinene kuti Iye adali mngelo wamba wa Yehova kaya mwana wa Yosefe chabe. Ena amanena kuti Khristu adali chimodzimodzi ngati Adamu pamene anali padziko lapansi angakhale kuti izi sizingapezeke penapaliponse m’Baibulo. Tiyenera tibvomereze kuti Adamu adalengedwa ndi Mulungu kuchokera ku dothi pamene Yesu, analengedwa komanso anabadwa Yekha ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera imene inamukuta Maria nakhala ndi pakati ngakhale anali asanadziwane ndi mwamuna wina aliyense. Choncho, Yesu anali ngati ife wobadwa mwa mkazi ngakhale kuti Iye analibe bambo wa uthunthu mu umunthu komabe Iye anabadwa monga ifeyo timabadwira. Tikudziwa kuti nkobvuta kumvetsetsa kuti munthu ngati ine ndikhale wangwiro, wopanda banga ngati Yesu ndipo nchifukwa chake, anthu ambiri lero alibe chidwi chokwanira ndi Khristu poteronso, sangathe kukwaniritsidwa mmaganizo pochita monga Yesuyo anachita kuti iwo eni apulumutsidwe mchikonzero ngati chimenechi.

Nchobvutadi lero kwa anthu ambiri kuti amvetse zoti munthu wooneka ngati ife akhale opatulika mwapadera, osachimwa, napirira mmayesero, nasiyana ndi ife mkhalidwe lake ndi maganizidwe ake. Pokhapokhapo ife titazama

m'Mau a Mulungu, tidzazindikira kwakukulu Mauwo, ndipo adzakhazikika mwaife ndikusintha chikhalidwe komanso zina zonse mmoyo wathu watsiku ndi tsiku motero, tidzatha kuona Yesu weni weni osati amene tikumudziwa tisanamvetse bwino Mau ake ayi. Mnjira imeneyi, chikhulupiriro chatu chidzakula nichibweretsa ludzu lalikulu ndi njala ya Mau ake kunthawi zosatha. Sitidzaonanso mosiyana kuti ena akhulupirire kuti Yesu ndiye Mulungu zimene zingachepetse Ukulu wake pamene anagonjetsa tchimo mu umunthu wake. Tonse tidzamva mofanana tikadzipereka.

Iye adali ndi uthunthu wa umunthu, anagawana nafe chibadidwe cha utchimo (A Hebri 4:15) koma anakwanitsa popirira nadzipereka kugonjetsa mayeserowo popempha kwa Mulungu kuti cholinga chake chikwaniritsike nachita chifuniro chake. Ndipo ichi Mulungu anamuthandiza koposa koteru, *“..Mulungu anali mwa Khristu, alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye Yekha”* (kudzera mwa Yesu Khristu – 2 Akorinto 5:19).

8.2 KUSIYANA PAKATI PA MULUNGU NDI YESU KHRISTU

Pali kugwirizana pakati pa ndime zimene zimakamba motsimikiza ndi motsindika za *“...Mulungu kukhala mwa Khristu”* ndi ma nunsu amene amanena za uthunthu ndi umunthu wa Khristu. Sichanzeru choncho, kutamira chiphunzitso chonena kuti Khristu analinso Mulungu chifukwa pali umboni wokwanira m'Mau a Mulungu kuti Yesu anangokwezedwa mwachisomo mcholinga cha Yehova Mwini wake. Maganizo onena za Yesu kuti adali Mulungu anaperekedwa komanso kubvomerezedwa pa msonkhano umene unachitikira ku Nicea mchaka cha 325 A.D.. Akhristu ambiri panthawiyi kunali koyamba kumva za nkhani yotere ndipo anali odabwa. Mwaona kale mmbuyomu kuti Mau oti *“mmodzi mwa atatuwo (trinity)”* sangapezeke pena pali ponse m'Baibulo. Tiphunzira zambiri zokhudza chigonjetso cha tchimo ndi Khristu mothandizidwa ndi Mphamvu ya Mulungu m'Phunziro 9. Koma chachikulu, tiyeni tikumbukire kuti chipulumutso chimadza pozindikira moyenera za Yesu Khristu weni weniyo (Yohane 3:36; 6:53; 17:3). Tikadziwa

chigonjetso chimenechi cha Yesu mozindikira bwino ndi moyenera, tikhoza kubatizidwa kotero, ifenso tikwaniritse chilamulo ndi kupeza nawo chipulumutso mwa Khristuyo.

Ina mwa ndime zimene zimaonetseratu kugwirizana pakati pa Mulungu ndi Yesu ndiyo 1 Timoteo 2:5: **“Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi** (mlumikizi!) **mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Khristu Yesu.”** Poganzira mau amene atsekedwa mizere mmunsi mwaowo, tikhoza kuona ndi kuzindikira bwino popanga mfundo zotsatirazi:

- ◆ Pokhalapo Mulungu mmodzi, sizingathekenso kuti Yesu adali Mulungu wina; Ngati Yehova ndi Mulungu ndipo Yesu nakhala Mulungunso, ndiye kuti pali milungu iwiri. **“...Koma kwaife kuli Mulungu mmodzi, Atate amene zinthu zonse zichokera kwa Iye”** (1 Akorinto 8:6). **“Mulungu Atate”** choncho, ndiye Mulungu, Yehova Yekhayo wolenga zonse za mdziko. Motero, nkosathekansa kuti pangakhale Mulungu winanso pamwamba pa ameneyu nakhala **“Mulungu Mwana”** monga ena amanenera. Tionanso kuti angakhale Chipangano Chakale chikutiiza ndithu kuti Yehova Mulungu ndiye mmodzi amene ali Atate (Yesaya 63:16; 64:8).
- ◆ Popitiriza pankhani imeneyi ya Mulungu mmodzi, pali Mlumikizi (onani kuti Baibulo la Chichewa linamasuliridwa kuti ‘mtetezi’ limene siliri tanthauzo lolondola keini kweni) amene ali munthu Khristu Yesu – **“..ndi Mlumikizi** (nkhoswe) **mmodzi..”** liwu limeneri likuonetseratu kusiyana pakati pa Mulungu ndi Khristu Yesu chifukwa olumikiza sangakhalenso wolumikizidwa.
- ◆ Khristu ngati **“nkhoswe”** ndiye amene achita uphungu, alumikiza ife ndi Mulungu. Iye amalumikiza pakati pa anthu ochimwa (ife) ndi Mulungu amene ali Opatulika, Wopanda banga ndi Woyera. Mulungu sangadzichimwire kwa Iye Yekha; kotero, zinatengera munthu wosachimwa koma wokhala nawo umunthu wochimwa (ndiye Yesu) kutilungamitsa kuchiyero. Ndipo uyu anali Yesu Khristu Yekha Mwana wa Mulungu amene anakwanira pa chikonzero chimenechi cha Mulungu. Ngakhale titaonetsetsa apa, Paulo sakunena kuti **‘Mulungu Khristu Yesu’** ayi.

Nthawi zambiri timakumbutsidwa kuti **Mulungu saali munthu** (Numero 23:19; Hosea 11:9); ngakhale kuti Khristu akunenedwa momveka bwino kuti

'Mwana wa munthu' mChipangano Chatsopano ndinso *'munthu Khristu Yesu'*. Iye anali *"Mwana wa Wammwambamwamba"* (Luka 1:32). Mulungu ngati *'Wammwambamwamba'* zitionetsa kuti ali Yekhayo amene anali, ali ndipo adzakhala *'Wammwambamwamba'*; Yesu ngati mwana wake, *"wa Wammwambamwamba"* awonetsera kuti sangakhale Mulungu wina mu uthunthu wa umunthu. Ndipo tikaona mau oti Atate ndi Mwana ponena za Mulungu ndi Yesu, nzowonekeratu kuti palibe kufanana. Zimathekadi kuti bambo ndi mwana amafanana mmaonekedwe ndi mzinthu zna koma zimenezi sizingatanthauze kuti angakhale mmodzi yemweyo ayi, komanso kuti angafananiretu mpaka zaka za kubadwa ayi. Mnjira imeneyi, pali kusiyana kwakulu pakati pa Mulungu ndi Yesu chomwe chionetsanso kuti Yesu sakufanana ndi Mulungu Mwini: Onani zimenezi mndime zomwe zapatsidwa mmunsizi pofananiza pakati pa Mulungu ndi Yesu:

MULUNGU

YESU

"..Mulungu sakhoza kuyesedwa"(Yakobo 1:13)

Mulungu samafa – Iye ndiosafa
mwachikhalire [kunthawi zosatha]
(Masalmo 90:1; 1 Timoteo 6:16)
Mulungu samaoneka ndi maso athu
(1 Timoteo 6:16; Eksodo 33:20).

"Wayesedwa mzonse monga ife"
(A Hebrai 4:15)

Yesu Khristu anafa kwa masiku
atatu (Mateyu 12:40; 16:21)
Anthu anamuona Yesu ndipo ena
anamugwira (1 Yohane 1:1
akutsindika kwambiri pamfundo
imeneyi)

Pamene ife tiyesedwa, timayenera kusankha pakati pa tchimo kapena kuchita zolungama ndi kumvera Mulungu. Nthawi zambiri, timapezeka kuti tasankha molakwika osamvera Mulungu. Khristu anali ndi zinthu zones zimenezi kuti asankhepo chimodzi ndipo mwamwayi, Iye anasankha chilungamo namvera Mulungu. Choncho, zikanatheka Khristu kusankha molakwika nakhala osamvera Mulungu koma Iye sanatero ayi. Tionenso pano kuti nzosayenera komanso zosatheka kungoganiza chabe kuti Mulungu angachimwe. Achimwa bwanji popeza Iye anakonza kale zolinga zake. Taonetsa kale kuti mbeu ya Davide imene inalonjezedwa pa 2 Samueli 7:12-16 ndi imenso idali Khristu. Ndime ya 14 ikunenetsa kuti Khristu akanatha kuchimwa: “...*akachimwa ndidzambulanga...*”

8.3 UTHUNTHU WA YESU

Liwu loti “*uthunthu*” likunena za mmene munthu aliri. Tinakambapo m’Phunziro 1 kuti Buku Loyera limanena za mauthunthu awiri – ndiwo a Mulungu ndi umunthu. Monga mwachilengedwe, Mulungu sangafe ndipo sayesedwa. Nzowonekeratu kuti Khristu sanali nawo uthunthu wa Mulungu pamene anali panso pano. Kotero, anali mu uthunthu wofanana ndi waife anthu. Mnjira yomweyi, Khristu sakanakhala ndi mauthunthu awiri nthawi imodzi. Mwaichi, kunali koyenera kuti Iye ayosedwe monga ife timayesedwe nthawi ndi nthawi (A Hebri 4:15), ndipo apa kuchokera mkuyera kwake, popirira mkuyesedwako, akanathadi kutilondolera kuchikhululuko. Zilakolako zathu zimene ziri mayesero athu mkati mwaife eni ndizo mayesero athu (Marko 7:15-23; Yakobo 1:13-15). Kunali kofunikira komanso koyenera choncho, kuti Khristu akhale muuthunthu wa umunthu ndipo motero, adzionere yekha nagonjetsa mayesero onse amene ankamufikiranso munthu.

Pa A Hebri 2:14-18 tikuwerenga chifupikitso chamau amenewa motere:

***“Popeza tsono ana (ife) ndiwo a mwazi ndi nyama (uthunthu)
Iyenso (Khristu) momwemo adalawa nawo makhaliidwe omwewo
(authunthu) kuti mwaimfa akamuononge iye amene anali nayo***

mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi;...Pakuti sanabvala Iye uthunthu wa maonekedwe wa angelo; koma anabvala uthunthu wa maonekedwe a mbeu ya Abrahamu. Potero, kudamuyenera kufanizidwa ndi abale mzonse, kuti akhale Mkulu Wansembe wachifundo ndi wokhulupirira mzinthu za kwa Mulungu, polumikiza mwachilungamo anthufe ndi Mulungu mchikhululukiro cha zoipa zathu. Pakuti popeza adamva zowawa, poyesedwa yekha, akhoza kuthandiza iwo amene ayesedwanso.”

Nunsu imeneyi ikutsindika kwamphamvu kuti zowonadi Yesu adali muuthunthu wa umunthu. **“Iye Yekha momwemo”** adalawa nawo (A Heberi 2:14). Onani kuti ndime imeneyi yangogwiritsa ntchito mawu atatu okha omwe aperekeratu chithunzi chonse ndi cholinga cha Khristu Yesu motsimikizira. Pa A Heberi 2:16 timvanso motsindika kuti Yesu sanabvala uthunthu wofanana ndi wa angelo ayi, powona kuti anali mbeu ya Abrahamu, amene anadza kudzapulumutsa namtindi wa okhulupirira nasandulikanso mbeu ya Abrahamu. Chifukwa chaichi, kudayenera kuti Yesu Khristu abvale uthunthu wa umunthu. **“Mzonse kudayenera kwa Iye kufanana ndi abale ake”** (ife – pa A Heberi 2:17) koteronso, tipeze chikhululukiro kwa Mulungu kudzera msembe yoperekedwa ndi Yesu Khristu. Pamene tikunena kuti Yesu sadakhalepo muuthunthu ngati wathu koma anali Mulungu mwana choncho, tidzitsutsa tokha komanso titsutsana ndi Uthenga Wabwino umene Khristuyo anafikitsa pakati pathu.

Onse amene anabatizidwa akachimwa, amayenera kufika chifupi ndi Mulungu mwakupemphera, polapa machimo awo mwa Yesu Khristu (1 Yohane 1:9); Mulungu amadziwa kuti Khristu analowa mkuyesedwa monga iwo ndipo kuti asiyana ndi Khristu popirira komanso kugonjetsa mayesero awo. Chifukwa chaichi, **“Mulungu mwa Khristu adzatikhulukira”** machimo athu (Aefeso 4:32). Nkofunika choncho, kumvetsa ndinso kulola kuti Khristu analowa mkuyesedwa mu uthunthu waumunthu monga ife tiri ndipo kuti tikachita monga Khristu anachita, koma tidzakwanitsa. A Heberi 2:14 akunenetsa kuti Yesu anayenera kukhala nawo mnofu ndi mwazi kotero kuti zonsezi zitheke kuchitika. **“Mulungu ndi Mzimu”** (Yohane 4:24) muuthunthu wake motero, ngakhale ali ndi thupi la ‘uzimu’ alibe mwazi ndi mnofu. Khristu pokhala ndi

mnofu komanso mwazi, anawonetseratu poyera kwaife kuti sanali ndipo si Mulungu kotero kuti safanana naye.

Dziwani kuti anthu ambiri akhala akuyesayesa kusunga Mau a Mulungu pofuna kuthana ndi mayesero osiyana siyana koma izi zimawakanika. Kotero, **“Mulungu anatumiza Mwana wake wa Iye Yekha mchifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa chauchimo, natsutsa uchimo mthupi”** (Aroma 8:3).

Tchimo liwonetsa chikhalidwe chachibadidwe cha umunthu wathu. Ife kawiri kawiri timafowoka ndi chilakolako chimenechi motero, **“mphoto ya uchimo ndi imfa”**. Kuti tichoke msinga zimenezi padafunikira chithandizo chochokera kwina kwake chifukwa ife patokha sitikadatha. Mnofu sudzakwanitsa kupulumutsa mnofu unzake. Mulungu choncho, anadumphirapo, natumiza Mwana wake amene anabadwa mu mnofu nakhala ndi mwazi ngati mmene ife tiliri, nakhala nalo khalidwe lauchimo mwa Iye. Koma mosiyana ndi ife, Iye anakwanitsa kugonjetsa mkuyesedwa kwina kulikonse angakhale kuti anali nacho chiganizidwe ndi chikhalidwe chauchimo. Aroma 8:3 afotokozera bwino za **“uthunthu waumunthu”** wa Yesu. Paulo walongosolanso kale mndime zoyambirirazo kuti **“mnofu ulibe chabwino”** ndipo kuti umatilekanitsa ife mkulunjika kwa Mulungu (Aroma 7:18,23) posamvera Iye. Chifukwa cha mnofu umenewu, ife sitikhoza kupulumutsidwa mkumangika kwathu kotero, kubwera kwa Khristu mu mnofu ndi mwazi, Yesu anadziwanso za kuperevera kwa uthunthu muumunthu wathu ndi kufowoka kwathu, nchifukwa chake, Iye anathanso kugonjetsa tchimo. Chotsatira chake, anatchulidwa **“M’phunzitsi Wabwino”**. Komabe Iye popitiriza kukana izi ananena: **“Unditchula Wabwino bwanji? Palibe Wabwino koma mmodzi ndiye Mulungu”** (Marko 10:17,18; Mateyu 19:17). Nthawi ina anthu ena ambiri anamuyamikira, nakamba zabwino zambiri zimene anachita pochiritsa anthu ndi kuchita zozizwitsa zambiri, Khristu sanatengerepo mwayi kudzitukumula ponyadira zimene iwo ananena ayi. Ichi nchifukwa chakuti **“..anadziwa zonse Iye Yekha chimene chinali mwa munthu”** (Yohane 2:23-25). Chifukwa cha kuzindikira kwakukulu kumene Iye anali nako pa munthu, Khristu sanafune kuti anthuwo azimuyamikira, namupembedza ngati kuti Iye ndiye Mulungu ayi. Iye panthawiyo anali munthu mu uthunthu ndi umunthu wamachimo.

8.4 UMUNTHU WA YESU

Ndime Zambiri za m’Baibulo zimaneneratu momveka bwino kuti Yesu Khristu anali mu umunthu. Kunalembedwa kuti Iye ankatopa, ndipo kuti nthawi ina mpaka anakhala pansi napempha madzi pa chitsime naamwa (Yohane 4:6). **“Yesu analira”** pamene anauzidwa zaimfa ya Lazaro (Yohane 11:35). Ndipo mongotsendera pamenepa, Khristu anamva zowawa zochuluka paimfa yake ya pamtanda chomwe chinaonetsadi umunthu wake. Iye anabvomereza ponena kuti: **“Moyo wanga ubvutika tsopano”** (Yohane 12:27), uku kunali kupemphera kwa Mulungu ndipo penapake mpaka anachita mantha napempha kuti imfayo imutalikire; **“...napempha nati, Atate, ngati nkutheka chikho ichi chindipitirire ine; koma simonga ndifuna Ine, koma Inu”** (Mateyu 26:39). Izi zikuonetsanso kuti zilakolako za Yesu ndi zofuna za Mulungu zinali zosiyaniranatu.

Mnthawi yonse ya moyo wake, Khristu anadzipereka kwa Mulungu pokonzekera tsiku limeneri lomaliza laimfa yapamtanda: **“Sindikhoza kuchita kanthu kwa Ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza, ndipo maweruzidwe anga ali olungama; chifukwa kuti sinditsata chifuniro changa, koma chifuniro cha Iye wondituma Ine”** (Yohane 5:30). Kusi yana kumeneku kwa chifuniro cha Mulungu ndi Khristu Yesu kutitsimikiziradi kuti Yesu sindiye Mulungu. Iye anali wotumidwa chabe osati Mulungu ayi.

Mmiyoyo yathu yonse, ife timayenera kukula mnzeru za chifuniro cha Mulungu, pophuzira mmayesero amoyo wathu watsiku ndi tsiku. Ndipo mwaichi, Yesu ndichitsanzo chathu chachikulu. Iye anaphunzira kumdziwa Mulungu mmoyo wake. Kuchokera mu umwana wake, **“Yesu anakula m’nzeru ndi mu msinkhu”** (Aefeso 4:13), ndi **“..mchikondi cha Mulungu ndi munthu”** (Luka 2:52). **“Ndipo Mwanayo anakula, nalimbika, nalikudzala ndi nzeru muuzimu”** (Luka 2:40). Tiona kuti ndime zimenezi zikukamba zoti kukula mnzeru ndi mu msinkhu zinkachitikira limodzi komanso motsagana. Kukula kunaoneka ndi

anthu mwa Iye muuzimu wake ndi mu msinkhu wake. Yesu akanakhala kuti ndi Mulungu, zonsezi sizikanaoneka ayi. Onaninso ichi kuti, pomaliza pamoyo wake wapadziko lapansi, Khristu anabvomereza kuti Iye sadziwa za tsiku limene Iye adzabwerenso padziko lapansi lino ndipo anatsimikizira kuti adziwa ichi ndiye Mulungu Yekha. (Marko 13:32).

Kumvera Mulungu ndicho chinthu chimodzi chofunikira kwaife kuti tichiphunzire kokwanira. Yesu anadutsa monsemo mnjira yomvera ngati mmene mwana wina aliyense ayenera kuchita pomvera bambo wake. **“...angakhale anali mwana, anaphunzira kumvera izi** (kumvera Mulungu) **adamva kuwawa nazo; ndipo popangidwa Woyera** (muuzimu) **anakhala wachilembo cha chipulumutso”** chifukwa anali atamaliza kukula kwake muuzimu (A Hebra 5:8,9). Afilipi 2:7,8 (kupitiriza ngati ndemanga ya Mpatuko 27) timva potsindika za kukula muuzimu pamene Yesu anakula kudzera muimfa ya pamtanda. Iye **“...anadzikhuthula, nadzichepetsa yekha, nakhala womvera...mpaka imfa yapamtanda”**. Mauwa akuonetseratu kuti Yesu anapitiriza kukula muuzimu, podzichepetsera chepetsera pamene anakula mu msinkhu ndi muuzimu mpaka pamene anamaliza kumvera Mulungu naafa, napachikidwa pamtanda. Apa mpamene **“anakhala Wangwiro”** chifukwa analolera mkupirira mmazunzo.

Zikuonekeratu apa kuti ntchito za Khristu ndi zimene zinamuyenera Iye kukhala Wangwiro ndi Woyera; Iye sanaumirizidwe kuchita izi ayi koma mwakuzindikira kwa Iye Yekha. Motero, Yesu anatikondadi ife, nadzipereka pamtanda paja chifukwa cha chikondi chimene Iye anali nacho paife. Kutsindikira kwa chikondi chimenechi cha Yesu mwaife sikukanakhala kwa phindu ngati Yesuyo akanakhala kuti anaumirizidwa ndi Mulungu (Aefeso 5:2,25; Chibvumbulutso 1:5; Agalatiya 2:20). Mulungu ndi wachifundo ndipo sanafuna kuchita ichi. Ngati Yesu anali Mulungu kotero, sizikanatheka kuti akhale opanda mwayi kusankha ndi chiyero mpaka kufa pamtanda paja ayi. Kutu Yesu adali ndi mwayi umenewu osankhawu, zitipatsa mphamvu ndi chilimbitso ife ndipo motero, ubale wathu ndi Khristu ukhala waukulu ndi opambana mchisomo chake.

Mulungu anakondwa powona kudzipereka kwa Yesu pamene anachita zonse mosaumirizidwa **“Chifukwa chaichi, Atate andikonda Ine chifukwa nditaya Ine moyo wanga, palibe wina andichotsera uwu, koma ndiutaya mwa Ine ndekha...”** (Yohane 10:17,18). Pamene Mulungu asangalatsidwa ndi kudzipereka komanso kumvera kwa Khristu, ndicho chowonekeratu kuti Khristu sanalinso Mulungu koma kuti analongosola umoyo wake m’Chiyero angakhale adali mu uthunthu wa umunthu (Mateyu 3:17; 12:18; 17:5). Ndipo apa paonetsanso kuti Khristu akanatha kumchimwira Mulungu.

KUNALI KOFUNIKA KUTI KHRISTU APULUMUTSIDWE

Chifukwa cha uthunthu wa umunthu wa Yesu, Iye ankadwalanso, ankatopa ndi zina zotero zimene zinkamuchitikira monga ife lero. Choncho, zionetsa kuti akanakhala kuti Yesu sanafe pamtanda paja, Iye akanafabe mwachitsanzo, mwina ndi matenda ena kapena ukalamba. Izi zikanachitika monga zimakhallira ife kapena kudzera mmatenda. Motero, Yesu anasowanso chipulumutso monga ife ndipo anayenera kupulumutsidwa ndi Mulungu. Podziwa izi. Yesu **“..anapereka mapemphero ndi mapembedzero ake pamodzi ndi kulira kwakukulu ndi misozi kwa Iye (Mulungu) amene anakhoza kumupulumutsa Iye (Yesu) muimfa, ndipo anamveka popeza anaopa Mulungu”** (A Hebri 5:7). Kungowona kuti Yesu anapemphera, napembedzera kwa Mulungu kuti apulumutsidwe kuimfa, zitipatsiratu chithunzi thunzi kuti Iye sangakhale Mulungu. Iye atafa naukitsidwa, **“...imfa siyidzachitanso ufumu mwa Iye”** (Aroma 6:9), kuonetsanso kuti poyambapo imfa inkachita ufumu (kulumulira) mwa Iye.

Ndime zambiri m’Masalmo zinalosera za Yesu; Mavesi ena m’Masalmo analembedwanso mmavesi a mChipangano Chatsopano ponena za Iye. Pali ndime zina ndithu zimene zimafotokozera kuti Yesu anayenera kufunafunanso chipulumutso cha Iye Mwini motsindika:

- analosera za kupachikidwa pamtanda kwa Yesu Khristu (Mateyu 27:34); Buku lonse la Masalmo 69 limakamba za maganizo a Khristu pamene anali pamtanda paja: ***Ndipulumutseni Mulungu... Yandikirani moyo wanga ndikuuombola...Chipulumutso chanu, Mulungu chindikweze pamsanja*** (vs.1,18,29).

•
changa” Mapemphero a Khristu kwa Mulungu ponena za chipulumutso chake anamveka; anamveka chifukwa chodzipereka kwa Iye pa zauzimu, osati chifukwa chakuti anali Mulungu mmodzi mwa atatuwo ayi (A Hebri 5:7).

Kuti Mulungu anaukitsa Yesu namukweza mkusafa nzosachita kufunsa ndipo iyi inali mfundo yofunikira koposa mChipangano Chatsopano:

“Mulungu ...anaukitsa Yesu...ameneyu Mulungu anamkweza ndi dzanja lake lamanja, akhale Mtsogoleri (Mfumu) ndi Mpulumutsi” (Machitidwe 5:30,31).

“Mulungu ... analemekeza Mwana wake Yesu... amene Mulungu anamuukitsa kwa akufa” (Machitidwe 3:13,15)

“Yesu ameneyo, Mulungu anamuukitsa;” (Machitidwe 2:24,32,33).

Yesu payekha anadziwa izi ndipo anaonetsa kuzindikira kwake pamene anapempha Mulungu kuti alemekeze Iye (Yohane 17:5 cp. 13:32; 8:54).

Ngati Yesu anali Mulungu kotero, ndime zonsezi zikanakhala zosafunikira kuti zilembedwe m’Buku Lopatulika. Tikudziwa tonse kuti Mulungu saafa choncho, ngati Yesu adali Mulungu, sakanafuna chipulumutso. Kuti anali Mulungu amene anaukitsa Yesu, zitionetsera kuti nzosiyana ndi zimene anthu amanena pa ukulu wa Mulungu poyerekeza ndi Yesu. Motero, nkosatheka kuti Khristu anali Mulungu monga mwa maulaliki ena.

8.5 UBALE UMENE ULIPO PAKATI PA MULUNGU NDI YESU

Tikangowona kuti Mulungu anaukitsa Yesu, zimatipatsa ife chilakolako, cholinga ndi nthumazi yoganizira za ubale umene ungakhalepo pakati pa Mulungu ndi Yesu. Kodi Yesu ndi Mulungu mmodzi mwa atatuwo? Ngati ndi ofanana

'amuyaya ndi mmodzi mwa atatuwo,' ndiye kuti ubale wao ndi umodzi wao sunganyemeke. Motero, sizingatheke kuti mwa chinthu chimodzi chomwecho china chife pamene gawo lina liri moyo ayi. Ubale weni weni pakati pa Mulungu ndi Khristu ufanana moyerekeza ndi ubale umene ulipo pakati pa mwamuna ndi mkazi m'banja: **"...Koma ndifuna kuti mudziwe, kuti mutu wa munthu yense ndiye Khristu; ndi mutu wa mkazi ndiye mwamuna; ndipo mutu wa Khristu ndiye Mulungu"** (1 Akorinto 11:3). Monga mwamuna amatsogolera banja, koteronso Mulungu amatsogolera Khristu angakhale kuti cholinga chawo nchimodzi. Monganso m'banja, cholinga chake chimakhala chimodzi nchifukwa chake, **"Khristu ali wa Mulungu"** (1 Akorinto 3:23), ngati mmene mkazi ali wa mwamuna wake.

Mulungu Atate motero, ndiye Mulungu wa Khristu. Tikamawerenga kuti **"Mulungu ndiye Atate wa Ambuye Yesu Khristu"** (1 Petro 1:3; Aefeso 1:17) angakhale kuti tikukamba pano Yesu anauka ndipo ali kale kumwamba, zitionetsera ndikulosera kuti ubale umenewu ulipodi mpaka lero monga mmene zidaliri Yesu asanafe nauka. Ena amanena kuti Yesu sanali ofanana ndi Mulungu panthawi yokhayo imene Khristu anali pansu pano. Dziwani kuti makalata onse a Paulo analembedwa Yesu atakwera kale kumwamba, ndipo mwaichi, popeza tawerenga kuti Mulungu ndiye Mulungu wa Ambuye wathu Yesu Khristu, ndiye kuti ichi sichinasinthidwe. Mulungu kotero, akadali mutu wa Khristu Yesu.

Buku la Chibvumbulutso linalembedwa patapita zaka 30 Yesu atalemekezeka kale komanso atakwera kumwamba komabe, mpaka lero Bukuli likukambabe kuti **"Mulungu wake (wa Khristu) ndi Atate wake"** (Chibvumbulutso 1:6 R.V.). m'Buku limeneri, Yesu woukitsidwayo, anapereka uthenga wake kwa okhulupirira onse. Akunena za **"...Mzati wa m'kachisi wa Mulungu wanga...dzina la Mulungu wanga, ndi la Mzinda wa Mulungu wanga..."** (Chibvumbulutso 3:12). Apa zikuonetseratu kuti ngakhale panopa Yesu amakambabe za Atate kuti ndiye Mulungu wake kotero, Khristu payekha si Mulungu ayi.

Pamene Khristu anali pansu pano mu uthunthu wathu uno, Iye ananena za Mulungu wake kuti ndiye Yekhayo. Khristu anali pansu pano mu uthunthu waumunthu wathu uno, Iye ananena za Mulungu wake kuti ndiye Yekhayo. Khristu anakambanso zokwera kumwamba: **"...kunka kwa Atate, ndi Atate wanu,**

ndi Mulungu wanga, ndi Mulungu wanu” (Yohane 20:17). Pamtanda paja, Yesu anasonyezeratu umunthu wake mokwanira: *“Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiraji Ine?”* (Mateyu 27:46). Mau amenewa sitingawamvetse pamene timva kuti Yesu akulandiridwa ndi Mulungu chifukwa Mulungu sangakhale ndi Mulungu wakenso. Ndipo pamene tiona kuti Yesu ankapemphera kwa Mulungu, *“Ameneyo, mmasiku a thupi lake anapereka mapemphero ake ndi mapembedzero pamodzi ndi kulira kwakukulu ndi misozi kwa Iye amene anali okhoza kupulumutsa Iye mwaimfa,”* (A Hebri 5:7; Luka 6:12). Tanena kuti Mulungu sangapemphere kwa Iye Mwini. Ndipo onaniso kuti ngakhale panopa, Khristu akupempherabe kwa Mulungu mmalo mwa mwaife eni kuti atipatse mwayi olapa (Aroma 8:26,27 NIV cp. 2 Akorinto 3:18).

Tsopano tapereka chindunji chonse chowonetsa ubale weni weni umene ulipo pakati pa Mulungu ndi Khristu Yesu komanso kuti palibe kusiyana pakati pa mmene ubale umenewu unaliri kalelo ndi lero lino. Khristu anamutchula Mulungu ‘Atate wake’ ndipo momwemo, ankapemphera kwa Iye. Mpaka pano, pamene Khristu anakwera kumwamba, izi ziri choncho. Pamoyo wake wadziko lino lapansi, Khristu anali kapolo, wantchito wake wa Mulungu (Machitidwe 3:13,26 NIV; Yesaya 42:1; 53:11). Yesu anatsindika ponena za Mphamvu ndi Ulamuliro umene Iye adali nawo kuti zonse ndizochokera kwa Mulungu, osati mwa Iye yekha ayi; *“Sindikhoza kuchita kanthu kwa Ine ndekha;...sinditsata chifuniro changa koma chifuniro cha Iye wondituma Ine. Mwana sakhoza kuchita kanthu pa Iye Yekha”* (Yohane 5:30,19).

MPATUKO 27: “POKHALA NAWO MAONEKEDWE A MULUNGU”

“Yesu...pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu; koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala mmafanizidwe a anthu” (Afilipi 2:5-11). Ndime izi zimamasuliridwa ngati kuti Yesu anali Mulungu, ndipo kuti pobadwa Iye anasanduka munthu. Ngati izi zingakhale zowona, ndiye kuti zonse zimene

tafufuza m'Phunziro 7 ndinso 8 nzosathandiza ndipo kuti tataya nthawi yathu pachabe. Tidziwe mokumbutsana pano kuti ndime imodzi yokha siyingathe kutsutsa Baibulo lonse limene ndilowuziridwa ndi Mwini Mulungu. Mwina tikhoza kuona kuti ingakhale ndime yokhayo imene itionetsa kusowa kweni kweni pofuna kulumikiza mafotokozedwe a chindunji cha mmene Yesu anachokera kumwamba, kusiya kaye ulemerero wake wa Umulungu pokhala Iye Mulungu mmodzi mwa atatuwo, nadza kudzakhala munthu mwa Maria. Ndongomeko imeneyi ikusowa kwambiri mndimeyi. Tatiyeni tionere limodzi kafotokozedwe keni keni ka ndime imeneyi mmunsimu:

1. Pali nunsu zingapo mndime zimenezi zomwe zikuonetsa kutsutsana ndi ulaliki wonena za Mulungu mmodzi mwa atatuwo:
 - Mulungu “...*anamkweza Iye...nampatsa dzina limene liposa maina onse,*” (vs.9) Onani kuti dzina limene Mulungu anampatsa Yesu silinapose Iye Mulungu Mwini kapena kufanana naye ayi koma linaposa maina ena onse kupatula Mulunguyo. Izi ziyenera kutipatsa chithunzi thunzi chabwino kuti Yesu sali ofanana ndi Mulungu Atate komanso kuti Iye sanadzikweze yekha ayi. Taona kale kuti Khristu anakwezedwa pamene Iye anamaliza bwino ntchito yake pogonjetsa mphamvu ya tchimo padziko lapansi kenaka nakwera kumwamba.
 - Cholinga cheni cheni chonse cha Yesu podzipereka, nadzichepetsa komanso kuzunzika kenaka nakwezedwa ndi Mulungu chinali chofuna “...*kuchitira ulemu Mulungu* (amene ali) *Atate* (vs.11); kotero, sali ofanana ndi Iye amene ayenera kulandira ulemu.
2. Nunsu zawerengedwazi nzofunika kuziganizira mofatsa komanso mwauzimu. Paulo wakamba za maganizidwe a Yesu pa Afilipi 1:8. Tikabwerera mmbuyo pang'ono pa Afilipi 1:27, tiona kuti Paulo wayamba nkutikumbutsa za maganizidwe athu mmitima mwathu. Tikhoza kuwerenganso zimenezi pa Afilipi 2: “...*amoyo umodzi, olingalira mtima umodzi;...ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzake omposa iye mwini; munthu yense asapenyere zake za iye yekha, koma yense apenyereenso za mzake. Mukhale nawo*

mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Yesu Khristu,” Afilipi 2:2-5). Choncho Paulo akutsindika zaife lero kuti tizikhala ndi mtima wofanana ndi Yesu, umene unadzipeka pothandiza anthu ena. Ndipo ndime zina zikukambanso zambiri pa kudzichepetsa kwa Khristu kuti anationetsera popereka chitsanzo chake osati zakusinthika kwina kulikonse kwa uthunthu wake ayi.

3. Yesu anali “...*mmaonekedwe onga a Mulungu*”. Tafotokoza m’Phunziro 8.3 kuti Yesu anali muuthunthu wa umunthu kotero, sizikugwirizana ndi maganizidwe oti Khristu anali ofanana ndi Mulungu ayi. Timvetsetsenso pano kuti mamasulidwe a ma Baibulo ena ambiri anachitika pofuna kukwaniritsa zimene anthu omasulirawo amakhulupirira ndi zimene amafuna koterodi, tiyenera kufufuza mozama matanthauzo eni eni a mau athu mzilankhulidwe zimene tikumasulirazo ncholinga chakuti tizimvetsa bwino. Afilipi 2: 5-8 ndi chitsanzo chimodzi mwa ndime zimenezi.

Liwu la mchi Greek loti *‘morphe’* ndi limene lidalembedwa pamenepa ndipo likutanthawuza za umunthu mu uthunthu wathu mwaichi, lagwiritsidwa ntchito pa Afilipi 2:7 pokamba za *“maonekedwe a kapolo”*. Anali ndi maonekedwe a Mulungu koma anatengera uthunthu mu umunthu wa munthu wina aliyense. Maonekedwe a kapolo samasiyana ndi maonekedwe a munthu aliyense. Mndimeyi mogwirizana ndi zimenezi; tinganene kuti ngakhale Yesu Khristu anali wolungama, anali nawo mtima ndi maganizidwe onga a Mulungu, komanso kuti analolera kudzichepetsa monga kapolo. Paulo kenaka akutitsimikizira ndikutilimbitsa kuti tikhale omasuka muimfa ya Khristu pa Afilipi 3:8-11. Tigawane naye *“morphe”* umene Iye ali nawo omwense anatiwonetsa paimfa yake ija pamtanda. Sindiye kuti tingagawane uthunthu wa umunthu wake umene Iye anali nawo ayi koma maganizidwe a Iye ayenera kuti alowe mwaife ndipo tikhala nawo mpaka muyaya. Tiyenera kuchitapo kanthu kuti izi zitheke, ndiko kuzindikira mozama mau amenewa. Tiyeni tsono, tisinthe maganizidwe athu lero kuti tiyenezedwe kukhala nawo *‘morphe’* kapena tinene kuti maonekedwe ndi maganizidwe a Khristu Yesu mpaka imfa. *“Morphe”* mchi Greek, ndiko kunena kuti *‘maonekedwe ndi maganizidwe mu uthunthu,’* kapenanso *‘kufananiza maonekedwe’*. Anthunso nawo, amakambidwa kuti ndi (*ali ndi morphe*) ofanana ndi

Mulungu mmaonekedwe awo (2 Timoteo 3:5). Agalatiya 4:19 akunena za Khristu kuti “...*aumbika mwainu*” (okhulupirira). Chifukwa Iye anali olungama, naganana ndi Mulungu mmaganizidwe, Yesu anali *‘mmaonekedwe a Mulungu’* kotero ifenso tikhalianso ofanana ndi Iye ndi Mulungu. Mwaichi, sizinali zolakwika kuti Iye anazindikira kutidi anali muumodzi ndi Mulungu ayi, monga ifenso tiri, mu zina Iye ndi ofanana koma zina ngakhale Khristu amabvomereza kuti sali ofanana naye Mulungu Atate.

4. Yesu sanadzilemekeze koma mmalo mwake, anadzichepetsa pozindikira kuti anayenera kukwaniritsa ulosi wa Yesaya 53:12. Angakhale kuti ichi chinali chinthu chobvuta kuchikwaniritsa, Iye anakwaniritsa: “...*pakuti anathira moyo wake kwaimfa;*” Iye anadzichepetsa mpaka kukhala ngati kapolo popeza anawatumikira iwo amene anamutsata (Yohane 13:14), mwaichi, anawonetsera poyera ungwiro wake mpaka komalizira, naafa pamtanda ngati mbala (Mateyu 20:28). Yesaya 52:14 analosera za kuzunzika kwake ndi imfa ya Yesu yapamtanda, “...*nkhope yake yaipitsidwa ndithu, kupambana kwa munthu aliyense, ndi maonekedwe ake kupambana ana a anthu.*” Kudzichepetsa kotere, “...*mpaka imfa ya pamtanda*” nchimene chidachitika mu umoyo wake koteronso chiyenera kuchitikanso mmiyoyo yathu. Izi sizinachitike kwa Iye pamene ankabadwa ayi koma zinachita kubwera ali moyo kale. Taona tsopano za maganizidwe ake, kudzipereka ndi kudzichepetsa kwake; ndipo izi zonse zikhale chitsanzo chachikulu komanso chofunika kwaife anthu ake lero. Motero, ndime zimenezi zikutsindika za umoyo wake wa Khristu pamene anali panso pano mu umunthu wauthunthu wake, nadzichepetsadi ngakhale anali nawo maganizidwe a Mulungu komabe anazindikira zofunika kuchita nawo maganizidwe amenewa pofuna kuthandiza ndi kupereka chitsanzo pa chipulumutso chathu.
5. Ngati Khristu anali Mulungu poyamba, ndipo kuti anausiya ulemmero ndi uMulungu nadza panso pano monga ena amanenera, ndiye kuti uMulungu umenewu sanali nawo pamene anali padziko lapansi lino angakhale kuti ena amati anali nawobe. Bvuto limene tiri nalo ife anthu ndilo kumangokhulupirira mzinthu zonena kapenanso zopangidwa ndi munthu.
6. Potsiriza, pamene tiganizira mau oti “*pokhala mmaonekedwe a Mulungu*” tiyeni tione kuti mauwa sakukamba za pachiyambi cheni chenicho mwa

umuyaya mchi Greek. Machitidwe 7:55 ponena za Stefano akunena kuti “*..pokhala wodzala ndi Mzimu Woyera*” . Stefano anakhala wodzala ndi Mzimu Woyera kuchokera panthawi ina yake osati pachiyambi, kapena pamene iye anabadwa ayi. Panali nthawi yeni yeni pamene ichi chinayambika, Zitsanzo zina zikupezekanso pa Luka 16:23; Machitidwe 2:30; Agalatiya 2:14. Khristu “*..pokhala mmaonekedwe a Mulungu*” kotero, kutanthauzira kuti anali mmaonekedwe a Yehova mwamaganizidwe ake osati kuchokera pachiyambi ayi. Timamva kuti Khristu anakula mmaganizidwe ndi mu msinkhu.

PHUNZIRO 8: MAFUNSO

1. Kodi Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu ali mmodzi mwa milungu itatuyo?
2. Lembani mfundo zitatu zomwe ziwonetsa kusiyanana pakati pa Mulungu ndi Yesu.
3. Ndi ziti mwanjira zapatsidwazi zomwe zikuonetsa kuti Yesu anali wosiyana ndi ife wanthu?
 - (a) Sanachimwepo
 - (b) Anali mwana wobadwa Yekha ndi Mphamvu ya Mulungu mChiyero
 - (c) Iye sakadachimwa ngakhale zikadatani
 - (d) Anaumirizidwa kukhala Woyera Mtima ndi Mulungu
4. Ndi ziti mwanjira zapatsidwazi zomwe zikuonetsa kuti Yesu anafanana ndi Mulungu?
 - (a) Anali ndi uthunthu wa uMulungu pamene anali panso pano
 - (b) Anali ndi Mtima Woyera wofanana ndi Mulungu
 - (c) Iye ankadziwa zonse zomwe Mulungu ankadziwa
 - (d) Iye anali ofanana ndi Mulungu mzonse
5. Ndi ziti mwanjira zapatsidwazi zomwe zikuonetsa kuti Yesu anali ofanana ndi ife wanthu?
 - (a) Anayesedwa mzonse monga ife timayesedwa komanso anaona zonse zomwe ife timaona lero
 - (b) Anachimwa akadali mwana wamng'ono
 - (c) Iye anafunikiranso kulandira chipulumutso
 - (d) Anali ndi uthunthu waumunthu
6. Ndi ziti mwaziganizo ziri mmunsizi zomwe ziri zowona?
 - (a) Yesu anali ndi uthunthu Woyera ndi makhalidwe a Chiyero

- (b) Yesu anali ndi uthunthu wauchimo koma ndi makhalidwe a Chiyero
- (c) Yesu anali ndi magawo onse awiri a uMulungu weniweniyo ndinso umunthu weni weniwo
- (d) Yesu anali nawo uthunthu waumunthu wa Adamu asanachimwe

7. Kodi kukanatheka kuti Yesu achimwe? Fotokozani momveka bwino pa mfundo yanu?

Mukayankha mafunso'wa chonde tumizani ku imodzi mwa ma adiresi mwapatsidwa m'mapeji oyambirira a buku lino.

PHUNZIRO 9
NTCHITO YA YESU

9.1 CHIGONJETSO CHA YESU

M'phunziro lapitali, tinawonetsa momwe Yesu adaliri mthupi lake ngati lathu ndikutinso adayesedwa monga ife. Kusiya kwake pakati pa ife ndi Iye ndikwakuti adagonjetseratu tchimo; ngakhale adali ndi thupi lauchimo, nthawi zonse adaonetsa khalidwe langwiro. M'khalidwe wotere ndi umene tiyenera kutengera pochita monga Iye komanso kukhala chikhalidwe cha Iye. M'Chipangano Chatsopano mkhalidwe umenewu wa Khristu ukutsimikizidwanso motere:-

- "*Adayetsedwa mzonse monga ife, koma sanachimwa*" (AHebri 4:15).

- "*Sadachite uchimo. " Mwai Iye mudalibe tchimo.*" (2 Akorinto 5:21; 1Yohane 3:5).

- "*Sadachimwe, ndipo palibe choyipa cymene chinachokera mkamwa mwake.*" (**1 Petro 2:22**).

- "*Woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ife wochimwa, wakukhala wopitirira miyama.*" (**AHebri 7:26**).

Uthenga wabwino ukuwonetseratu mmene abwenzi ake adadziwira za mkhalidwe wake wangwiro, umenenso abwenzi akewo adadziwadi naona khalidwe lake langwiro, limene lidaonetsedwa kudzera mmawu ndi ntchito zake. Mkazi wa Pilato adamzindikira kuti anali "*wolungama*" (Mateyu 27:19), amene sadayenera kulangidwa; angakhale msilikari wa chi Roma ananena za Iye "*ameneyu anali munthu wolungama.*" (Luka 23:47). Yesu naye adawadzudzula a Yuda aja nati: "*Ndani wa inu anditsutsa ndi uchimo?*" (Yohane 8:46). Iwo motero, anasowa choyankha. Chifukwa cha chigonjetso chake changwiro mnjira zonse, Yesu wa ku Nazarene adakwezedwa kuposa Angelo (AHebri 1:3-5). Adakwezedwa kuposa maina onse (Afilipi 2:8). "*Dzina lake adzakhala Odabwitsa, wauphungu*" (Yesaya 9:6).

Ichi ndichodziwikiratu kuti Yesu sadapeze udindo umenewu Iye asanabadwe ndi kufa ayi koma pamene anagonjetsa tchimo. Chifukwa cha chigonjetso chake changwiro mnjira zonse, Yesu waku Nazarene adakwezedwa kuposa angelo (AHebri 1:3-5) Adakwezedwa kuposa maina onse (Afilipi 2:8) Dzina koteru “..adzakhala *Odabwitsa, Wauphungu...*” (Yesaya 9:6). Ichi nchodziwikiratu kuti udindo umenewu Yesu sadaupezedi Iye asanabadwe nafa ayi.

Mwaichi, chifukwa chakhalidwe lake langwiro, Mulungu adawonekera mwa Yesu (1 Timoteo 3:16). Ntchito ndi zolankhula zake zinawonetsera cholinga cha Mulungu. Iye anachita zonse monga mwa chilamulo cha Mulungu ndipo ife tiyeneradi kumachita zonse ngatidi kuti tikumuona Mulungu pamaso pathu ndipo kuti alidi pafupi nafe. Chotero, monga Yesu anali ngati kalilole wathu, chowonetsera cheni cheni cha Mulungu – “*chifaniziro cha Mulungu wosawonekayo*” (Akolose 1:15), ife tikhale mchifanifanicho, tichite monga mwachifanizo chakecho. Mwaichi, palibe chifukwa chakuti ife anthu timuwone Mulungu monga m'mene timawonera munthu wina aliyense. Monga momwe Yesu akunenera, “*iyе amene awona Ine wawona Atate; nanga munena inu bwanji, Tiwonetseni Atate?*” (Yohane 14:9). Malembo akutifotokozera motsimikiza kuti Mulungu Atate adawonetsedwa mwa Yesu Khristu Mwana wake (2 Akorinto 5:19; Yohane 14:10, Machitidwe 2:22) Omwe amaphunzitsa za utatu mwa mmodzi amati mwana adaonetsedwa mwa Yesu. Koma Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu adawonetsedwa mwa Yesu . Mau anasanduka kukhala thupi (Yohane 1:14), osati mau adalowa mthupi ayi.

Pamene tili mudziko lauchimo, ndikutinso tchimo lili munthupi lathu, ndi chinthu chovuta kuti timvetsetse mphamvu ya uzimu yimene khristu alinayo kuposa ife; kuti munthu wofanana ndi ife athe kuonetsa chilungamo chenicheni chamulungu m'makhalidwe ake. Kukhulupirira izi pafunika chikhulupiriro chenicheni kusiyana ndi kungovomereza kuti khristu anali mulungu ; Chikhulupiriro chautatu ndi chakutinso khristu ndi mulungu chiliponseponse chifukwa chili chosavuta kuchimvetsetsa.

Popeza Khristu adali ndi thupi ngati lathuli, Khristu adayenera kufa. Adali wobadwa ochokera mwa Adam podzera mwa Maria, ndipo ana onse a Adamu adayenera kufa (1 Akorinto 15:22) Ana onse a Adamu adayenera kufa chifukwa

cha tchimo , angakhale kuti anali olungama mwa Iye yekha. **“Imfa ilamulira ...kudzera mu chimo la munthu m'modzi** (Adam) **Kuchionongeko** (imfa) **...chifukwa cha kusamvera kwa munthu mmodzi onse ali ochimwa choncho ali oyenera kufa**”. (Aroma 5:14-19 cp; 6:23). Ngati mwana wa Adamu Khristu adali **‘ochimwa’** choncho kudayenera kwa iye kufa. Ngati momwe anali onse a Adamu adalangidwa kuti adzafa chifukwa cha Mulungu adampanga kukhala ochimwa chifukwa cha ife amene sadadziwa chimo (Akorinto 5:21).

Tikabatizidwa mwa Khristu, ndinjira yokhayo imene ingatitengere ku chipulumutso ndipo tidzathanso kukhala **‘mwa Khristu’** nitibvala kulungama kwake. Pobatizidwa timafanizidwa kukhala muimfa ndi mkuuka kwake kwa Khristu pamodzi ndi Iye (Aroma 6:3-5), komanso ndiyo njira yokhayo ya chipulumutso kuchoka kumachimo athu, poweruzidwa, ngakhalenso kuyesedwa wolungama pamaso pa Mulungu (Aroma 4:25).

Zinthu zofunikira zimene taziona pachigawo chimenechi zingakhale zopanda njira ngati ife sitibatizidwa. Pa nthawi ya ubatizo timadziphatikiza ndi mwazi wa Khristu umene udakhetsedwa pa mtanda; okhulupirira amachapa **“zovala zawo ndi kuziyeretsa mmwazi wa Mwana wa Nkhosa”** (Chibvumbulutso 7:14). Mophiphiritsa, ndiye kuti abvala zobvala zoyera, kuyimirira chilungamo cha Khristu chimene chidza kwa iwo (Chibvumbulutso 19:8). Ndipo nchapafupi kudetsa zobvalazi chifukwa cha tchimo lathu (Yuda vs.23); tikachimwanso titabatizidwa kale, tiyenera tigwiritse nchito mwazi wa Khristu, kudzichapanso popempha Mulungu kuti atikhululukire machimowo mwa Khristu Yesu. Koteronso tikabatizidwa, tiyenera tilimbike kuti tikhalire ndi mdalitso umene tidalowa kale. Mpofunika kuti tsiku lirilonse tizipeza kanthawi kapadera kodziyesa tokha pa zomwe tachita ngati nzabwino kapena ayi, ndipo tikazindikira kuti tachimwira Mulungu, tiyeni tipemphe chikhululukiro mkupemphera. Tikatero, tidzakhala olimba mtima, pakuti tidabvala chilungamo cha Khristu mpaka pamene Khristu Yesu adzabwera, ndi chiweruzo padziko lapansi (Afilipi 3:9). Kawirikawiri timanena za chikhulupiriro kuti chichokera mchilungamo, ndipo zikuonetsa kuti nkosatheka kupeza chipulumutso mwaife tokha ndi ntchito zathu; chipulumutso chidza mchisomo chake: Mchisomo ndife opulumutsidwa mwachikhulupiriro; koma osati mwa ife tokha ayi; Iyi ndiyo mphatso ya Mulungu; osati chifukwa cha ntchito zathu ayi (Aefeso 2:8,9).

Monga chiweruzo ndi chilungamo ziri 'mphatso' '(Aroma 5:17), chimodzimodzinso chipulumutso ndicho mphatso ya mtengo wapatali kwaife. Chifukwa cha ichi, machitidwe athu mu ntchito ya chi Khristu izikhala yoyamikira zomwe Mulungu amatichitira - amene akutiwona ife olungama mwa Khristu, ndikutipatsa ife njira ya moyo wosatha. Ndichinthu choopsa kwambiri kuti ife tiziganizira kuti tikachita ntchito iriyonse, ndiye kuti tidzapulumutsidwa. Ngati ziri choncho, ndiye kuti timadzinamiza: ndimphatso chabe ya Mulungu kuti ife tipulumutsidwe koteronso, sitingathe kupeza mwatokha, tiyenera tibvutikire, ndikubvomereza mwachikondi pomulemekeza modzipereka. Chikhulupiriro chenicheni chibala ntchito (Yakobo 2:17).

Yesu monganso ife, adabadwa mwa Adamu, ndipo analandira chilango chimenechi motero, ifenso tiyenera kulandira chilango ngati momwe analangidwa ngakhale kuti Iye sanachimwe pamene ife tonse tiri ochimwa. Kudayenera kuti Khristu afe popeza adali ndi thupi lauchimo ngati lathu, Iye adalandira nawo tembelero limene adalandira ana a Adamu mmunda muja. Ngakhale Iye payekha sanachimwe, Iye sanasemphe imfa koma anafa imfa yochititsa chisoni. Chifukwa cha ungwiro wake kotero, ***“Mulungu adamuukitsa kwa akufa kumuombola m’ imfayo, chifukwa sadayenera kuti akhale chifere”*** (Machitidwe 2:24). Khristu adalidi mwana wa Mulungu ndipo mphamvu ya Mzimu Woyera idamuukitsa kwa akufa (Aroma 1:4). Chonchotu, dziwani kuti izi zidatheka chifukwa cha khalidwe langwilo la Khristu, popeza Mzimu wake unali woyeretsedwa, Iye adaukitsidwadi muulemelo wa muyaya.

Khristu anafa pamtanda osati chifukwa chokhacho chakuti adali ndi thupi mu uthunthu ngati wathuwu ayi komanso kuti adafunsa Mulungu nadzipereka yekha ngati nsembe kotero, Iye ndiyo mphatso ya mtengo wapatali kwa ife; Iye adaonetsadi chikondi chake chachikulu chimene ali nacho kwa ife paimfa yake yapamtanda, nafadi chifukwa cha machimo athu (1Akorinto 15:3) podziwa kuti kupyolera mu imfa yake, onse okhulupirira mwa Iye akapulumsidwe kwathunthu kuimfa yosatha (Aefeso 5:2,25; Chivumbulutso 1:5; Agalatiya 2:20). Pachifukwa chakuti yesu adali wangwiro pamakhalidwe ake, chidali chosabvuta kwa Iye kugonjetsaa chotsatira chake cha tchimo ndipo anakhala munthu oyamba kuukitsidwa kwa akufa napatsidwa moyo wauzimu wa muyaya. Chimodzimodzi onse

amene amubvomereza Khristu pobatizidwa, nakhala umoyo wao onse ngati Khristu, iwo ali ndi chiyembekezo chodzaukanso ndi kupatsidwanso mphatso ngati imene Khristu Yesu anapatsidwa. Iye ndiye chitsanzo chopezeka cha moyo wosatha.

Tikazindikira ichi kuti zowona Khristu chidamuchitikiradi, nawuka kwa akufa, ndiye kuti tidzawonanso kufunika kwake kwa ife kuti monga Khristu, ife tidzaukanso kwa akufa mu ulemelero. Apatu pali chitsimikizo chakuti tidzaukitsidwa ndinso kuweruzidwa monga mwa mau (Machitidwe 17:31). Moteronso, ngati tikhala mchowonadi monga Iye, tidzalandiranso mphatso ya moyo wosatha, **“pakuti amene adaukitsa Ambuye Yesu, adzaukitsanso ife natipatsa mphamvu mwa Yesu Khristu”** (2 Akorinto 4:14; 1 Akorinto 6:14; Aroma 6:3-5). Ngati ife tiri ochimwa, ndipo sitilapa machimo athu pomutsata Yesu, tidzafa ndithu popeza mphotho ya tchimo ndiyo imfa (Aroma 6:23). Koma, pakuti Khristu adakhala wamoyo, chifukwa cha ungwiro wake, namvera Mulungu, mwakutero, imfa sidzakhalsanso ndi ulamuliro mthupi lathu. Mulungu adzatiukitsa, natipatsa ife mphatso ya moyo wosatha monga mwa chikonzero chake.

Mmalo mwa zotsatira zake zauchimo, Mulungu atilonjeza, **“chilungamo ndi moyo wosatha”** (Aroma 4:6) monga mwa mchikhulupiro cha malonjezano a chipulumutso chathu. Tikudziwa kuti tchimo ndi limene lidzetsa imfa choncho, ngati tikhulupirira mchowoonadi kuti Mulungu adzatipulumutsa ku imfayi, tiyeneranso kukhulupirira kuti Iye adzatiwona ife mkulungama kwathu. Khristu adali wangwiro; Ifenso tikhale a Khristu mchowoonadi motsata chitsanzo chake, ndipo Mulungu sadzatiyesa ochimwa pamaso pake, adzatifananiza ndi amene sadachite tchimo, ndiye Khristu; kotero kuti tikawoneke wolungama pamaso pa Mulungu mwa Iye amenenso tsopano ali wolungama (2 Akorinto 5:21); Izi zikutanthauza kuti tiyenera tikhale mwa Khristu pobadwanso mwatsopano. Tibadwa mwatsopano mu ubatizo ndikuyenda mu umoyo womwe Khristuyo adayenda nachita. Zitanthauzanso kuti **“mwa Khristu Yesu”** timayesedwa anzeru, ndi achilungamo chomwe mwaife chimabweretsa chiyeretso ndi chiwombolo mwa mwazi wake (1Akorinto 1:30,31); Onaninsu kuti mndime zimenezi, tikulimbikitsidwa kuti timudziwe ndi kumulemekeza Khristu pa zinthu zazikulu zimene adakwaniritsa mwaife: **“Mwa uthenga wabwino, chilungamo**

cha kwa Mulungu chaulidwa, chilungamo cha mchikhulupiriro (chadziwika kwaife)” (Aroma 1:17). Ngati timvetsetsa zimenezi, ndiye kuti tiri ndi **‘Uthenga Wabwino’** wa choonadi.

Zonsezi zidatheka kupyolera mkuuka kwa Khristu. Iye anali chipatso choyamba **“kwa anthu onse amene adzapatsidwe thupi losafa kudzera m’ntchito imene adakwaniritsa** (1Akorinto 15:20), **“oyamba kubadwa kubanja latsopano la uzimu omwe adzapatsidwe maonekedwe a Mulungu”** (Akolose 1:18; Aefeso 3:15). Kuuka kwa Khristu kwapereka mwayi wakuti okhulupirira mwa Khristu onse akawoneke ngati olungama, pakuti abvala kulungama kwake. Khristu **“adaperekedwa chifukwa cha mikwingwirima yathu, ndipo adaukitsidwa kutiyesa ife olungama”**. (Aroma 4:25).

Tizikhala ndi nthumanzi poganizira za chikhulupiriro chathu mzinthu ngati zimenezi kotero kuti Mulungu atiwonededwe ife angwiro ndi ogonja. Khristu adzatiweruza ife. Tiyeni kotero, **“tikhale wopanda chirema muulemelo wake”**, Iye akatiyimika ife natiyenera kukhala woyera, osasusutika pamaso pake (Yuda vs.24; Akolose 1:22; Aefeso 5:27). Ndichodziwikiratu kuti mthupi lathu lauchimo, ndikulephera kwathu muuzimu, timakhala olimbikitsidwa tikakhulupirira kuti Yesu ndiye chiwombolo chathu mzinthu zimenezi nchifukwa chake, tikaonetsetsa, ziphunzitsa zambiri angakhale ziripo pakati pathu, sizitha kufikapo pa chikhulupiriro chenicheni chimene Mulungu anatikonzera. Koma chimene chingatipatse chikhulupiriro cha choonadi cha kuuka kwa Khristu ndipo timvetsetsa ndikuzindikira, ndicho chokhacho chopezeka m’Baibulo ndipo tidzaonadi kuti; **“Mulungu ...adamuukitsa kwa akufa...mwakuti ndi chiyembekezo chanu** (mkuuka) **chikhale mwa Mulungu”** (1 Petro 1:21).

9.2 MWAZI WA YESU

Nthawi zonse timawerenga mChipangano Chatsopano kuti chiweruzo ndi chipulumutso chathu chiri mwa mwazi wa Yesu (Yohane 1:7; Chibvumbulutso

5:9; 12:11; Aroma 5:9). Kuti tidziwedi kufunika kwa mwazi wa Khristu, tiyenera kumvetsetsa momwe Baibulo linenera kuti *“moyo wa nyama zonse uli mmwazi”* (Levitiko 17:4). Popanda mwazi, thupi silingathe kukhala ndi moyo; choncho, mwazi ndicho chizindikiro cha moyo. Izi zikufotokozerera kuti popanda mwazi wake, simudzakhala ndi moyo " (Yohane 6:53).

Tchimo limadzetsa imfa (Aroma 6 :23); ndiye kunena kuti, kukhetsa mwazi kumene kudzetsa moyo. Pachifukwa cha ichi ana a Israeli ankeyenera kukhetsa mwazi nthawi zonse pamene achimwa pamaso pa Mulungu, chomwe chitikumbutsa kuti tchimo limadzetsa imfa. Pafupipafupi zinthu zonse mwa lamulo (la Mose) zikhululukidwa ndi mwazi: popanda mwazi kotero, palibe chikhululukiro (cha machimo - AHebri 9:22). Chifukwa Mulungu poyambapo adapha mwana wa nkhusa kuti apeze zikopa zoti zibise tchimo la Adamu kalelo (Genesis 3: 7,21), ifenso tifunafuna chilungamitso mwa mwazi wake wa Yesu Khristu. Chimodzimodzinso, nsembe ya Abele idabvomerezedwa kuposa ya Kaini amene adapereka nsembe ya zipatso, chifukwa Abele adalemekeza mfundo yotsatira chikhululukiro mwa mwazi wa mwana wa nkhusa. Izi zititsimikizira kuti popanda kukhetsa mwazi sipangakhale chikhululukiro cha machimo athu ndipo kuti Mulungu sangabvomereze (Genesis 4:3-5) mapemphero athu ngati sitidzera mwa Yesu Khristu.

Zonsezitu zinkanenera za zinthu zapamwamba ponena zakufunikira kwa mwazi wa Khristu. Pamene ana a Israeli anapaka mwazi wa nkhusa pa mphuthu za nyumba zawo asanatuluke mu utchimo (kwa Aegupto), zinalosera kuti Khristu adzayenera kupachikidwa pamtanda kuti machimo athu akhululukidwe ndipo kotero, tikayenerezedwe kulandira chipulumutso pamene takhulupirira. Mwaichi, tionanso kuti mwazi nsembe iriyonse m’Baibulo, umkanenera zodzachitika kutsogolo pamene Yesu adzatipulumutse ndi mwazi wake umene tsopano ukutiphimba pamaso pa Mulungu Yesuyo asanabwerenso. Kuti machimo ayeretse, malingana ndi cholinga cha Mulungu, kunayenera kukhetsedwa mwazi. Ngakhale zinali choncho, kukhetsa mwaziko kunayenera kupha nyama zomwe sizinkapereka chithunzi cheni cheni popeza amene anayenera kudzipereka adali munthu amene adachimwayo. Kotero nyama zija zidali chiphunzitsa

chabe. Sikunali koyenera kotero, kuti munthu aphe nyama nati ikhale ngati choyimira mmalo mwa imfa yake kapena kuti ikhale chenicheni choimirira imfa yake ayi. Nyama zimene ankapha sizimadziwa cholondola kapena choona ayi; Nchifukwa chake, mwazi wa nyama sukanatha kuchotsa tchimo kotero Yesu anadzipereka kuchotsa tchimo. "(AHebri 10:4). Tsono ziri choncho tikhoza kufunsa kuti kodi nchifukwa chiyani a Yuda ankapereka nsembe za nyama akachimwa? Paulo akutiyanika motere pa Agalatiya 3:24 "*...lamulo linali namkungwi kutilosera za kubwera kwa Khristu,*". Nyama zimene ankapha ngati zoperekerira tchimo zidali zopanda banga monga timawerenga pa Eksodo 12:5; Levitiko 1:3,10. Izi zinalosera kuti Khristu, ngakhale adzaphedwa, analibe tchimo lina lililonse. Khristu kotero, anali "*Mwana wa nkhusa opanda banga*" (1Petro 1:19). Khristu choncho, ndiye nsembe yeni yeni imene Mulungu adayidziwa kalelo kuti adzaipereka. Pachifukwa chaichi, Mulungu anatha kukonza ndondomeko ya chikhululukiro chamachimo angakhale Khristu anali asanabadwe. Imfa yake inali ndi cholinga ndi anthu padziko lapansi monga mwa chipangano chimenechi (AHebri 9:15). Tiwona kuti zonsezi zikutanthauzira maulosi a lamulo la Mose (AHebri 8:5-9). Msembe zonse zimene zinaperekedwa pansu pa lamulori koterodi, zinkalosera kubwera kwa Khristu, imene inali nsembe yodzipereka Iye yekha (AHebri 9:26; 13:11,12; Aroma 8:3; 2 Akorinto 5:21).

Tinafotokozanso m'Phunziro 7.3 kuti Chipangano Chakale chonse ponena za lamulo la Mose kuti lidaunikira Khristu. Lamulo la nsembe lidalinso ngati njira imodzi yopemphera kwa Mulungu podzera kwa 'Wansembe Wamkulu' amenenso adali nkhuswe pakati pa Mulungu ndi anthu. Motero, mBaibulo, tiri ndi mapangano awiri; lakale kudzela m'lamulo la Mose ndi latsopano mwa Yesu Khristu amenenso ali nkhuswe wa pangano latsopanoli (AHebri 9:15). "*Pakuti chilamulo chimaika akulu ansembe, anthu okhala nacho chifowoko; koma mau alumbiro amene anafika chitapita chilamulo, ayika Mwana woyesedwa wopanda chirema ku nthawi zonse*" (AHebri 7:28). Pachifukwa chakuti ansembe anali anthu ochimwa, sadali ndi mwayi opeza chikhululukiro chenicheni chifukwa anaonetsa kuti sanachifune. Iwo anasangalatsidwa ndi maulemu amene analandira ndinso Nyama zimene ankaotchazo. Chimene chidafunikira ndi munthu ngati iwo chinali kukhala

angwiro, amenenso akadatha kupindula nayo nsembeyo pophatikizidwa muimfayo. Chimodzimodzinso, wansembe wankulu wangwiro adafunika amene akadatha kupindula nayo pophatikizidwa kuimfayo. Motero, wansembe wankulu wangwiro adafunika akhale amene akadatha kumvera chisoni anthu ochimwa amene ankabweretsa nyamazo ndipo iye nawayimira ngati nkhoswe yawo (AHebri 2:14-18).

Yesu akukwanira kuposa wonse pachikonzero chimenechi – *“Pakuti Mkulu wa Nsembe wotere anatiyenera ife, woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wopatulidwa kumachimo...”* (AHebri 7:26). **Mkulu wa nsembe safunanso kupereka nsembe ya machimo ake, kapena kuti Iye adzafanso lero lino ayi** (AHebri 7:23,27). **Pakumvetsetsa malembowa, tikuona kuti Khristu ndiye Wansembe wathu:** *“Chonchotu akhoza kupulumutsa konsekonse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nawo moyo wake chikhalire wakuwapembedzera iwo.”* (AHebri 7:25).

Chifukwa adali ndi thupi laumunthu ngati lathuli, Khristu, ngati wa Nsembe wa Mkulu, *“...akhoza kumva chifundo ndipo ali odziwa kulakwa kwathu, popeza Iyenso anazingwa ndi chifowoko”* (AHebri 5:2). **Tikumbutsidwanso za Khristu kuti,** *“...Iyenso momwemo adalawa nawo makhaliidwe aumunthu”* (AHebri 2:14). **Monganso ansembe akulu a chi Yuda adali nkhoswe za anthu, nayenso Khristu ali wa nsembe wa Israel wa uzimu omwe ali anthu onse obatizidwa mwa Khristuyo, kotero, Iye ali nkhoswe yawo ngati iwo amvetsetsadi uthenga wabwino wa choonadi. Alitu** *“..wansembe pa nyumba ya Mulungu”* (AHebri 10:21), mmene muli anthu obadwanso kwatsopano mu ubatizo (1 Petro 2:2-5). **Anthuwa ndiamene ali ndi chiyembekezo chenicheni cha Uthenga Wabwino** (AHebri 3:6). **Pofuna kulemekeza ubwino wa unsembe wa Khristu, tiyeni tilolere uphungu wake pobatizidwa mdzina lake chifukwa popanda kutero, Iye sangakhale nkhoswe yathu.**

Tikabatizidwa mwa Khristu, tidzagwiritsa bwino ntchito ya umsembe wakewo chifukwa tikhala ndi udindo wapadera mu umoyo wathu; *“...mwa Iye tiyenera tipereke nsembe yolemekeza Mulungu nthawi zonse”* (AHebri 13:15). **Cholinga cha Mulungu potipatsa Khristu ngati wansembe wathu**

chinali chaku timulemekeze Iye; mnjira imeneyi, tiyenera kumulemekeza Mulungu mwa Khristu kunthawi zones za moyo wathu. AHebri 10:21-25 akunena za maudindo amene tili nawo mwa Khristu ngati Wansembe Wankulu: “.....tiri naye Wansembe Wankulu panyumba ya Mulungu”:

1. Tiyeni tidze kufupi (ndi Mulungu) ndi mtima owonadi mchikhulupiriro chenicheni, titachapa mitima yathu kuchotsa zoipa ndi madzi oti mbuu. Tikamvetsetsa unsembe wa Khristu motero, tibatizidwe mdzina lake pomvera malamulo ake (Kuyeretsa matupi athu), ndipo tikatero, tisabwererense kuzoipa mmaganizo ndi mzochita zathu nthawi zonse. Ngati takhulupirira kuti tifuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu kudzera mu nsembe yake pafunika tiwonetse kudzipereka kwathu.

2. Tiyeni tigwiritsitse chikhulupiriro chathu chimene tichionetsa posabwerera m'mbuyo. Tisabwewuke ku chiphunzitso choonadi chimene chatizindikiritsa unsembe wa Khristu.

3. Tiyeni tilemekezane wina ndi mzake ndi kudza ku choonadi. Powonjezera apa, tisasiyane ayi koma kukhalira pamodzi, ndi Iye. Tikhalenso pamodzi ndi onse amene amamvetsetsa bwino Bulu Loyera ndipo potero tidzapindula nawo mzeru zawo. Kuchita unsembe wa Khristu, timakwaniritsa cholinga cha Mulungu posonkhana nawo anzathu pamodzi pamene tidya nawo mgonero wa Ambuye, uku ndiko kukumbukira nsembe yeni yeni ya Khristu (onaninso Phunziro 11.3.5).

Ngati titsata zimenezi tidzakhala olimba pamene tikukonzekera pachipulumutso chathu. Tidziwe kuti pamene munthu abatizidwa, akhala mwa Khristu ndipo iyi ndi nthawi imene munthu amakumana ndi mayesero akulu. Potero timayenera kuyandikira pa Mpando wa Chifumu wa chisomo nthawi zonse kuti tingalowe mkuyesedwa. Ndipo tikatero, tidzakhala mchisomo cha akuthandiza anzathu nthawi ya kusowa (AHebri 4:16).

9.3 NSEMBE YA IFE NDI IYE YEKHA

Tiyenera kumvetsetsa za momwe Yesu Khristu adakhudzidwira ndi nsembeyi. Ndipo nchosakayikitsa kuti nsembeyi adaipereka kwaife ndikuti komaliza Iyenso naye adapindulapo. Tiyeneranso kuzindikira kuti ngakhale Yesu sadachimwe, adali ndi thupi mu uthunthu wa thuli la umunthu. Adagawana nafe zowawa zomwe munthu aliyense amene adabwera kudzamufera amakumana nazo. Monganso tanena kale pa mfundoyi kuti Khristu adayesedwa mzonse monga ife timayesedwa. Nayenso adafuna “Chipulumutso” kapena ‘kupulumutsidwa ku thupi la imfa limene tonse tiri nalo’. Izi zidanenedwa kale ndi aneneri Iye asanabadwe.

“Ndipereka mzimu wanga m'dzanja lanu: Mwandiombola inu Yehova, Mulungu wa choonadi” (Masalmo 31:5). Tikumbukenso kuti awa adali mau amene Yesu adalankhula pamtanda paja (Luka 23:46). Atate ake adali ngati muwombolo amene *“.....adzaombola moyo wanga ku mphamvu ya manda”* (Masalmo 49:15).

“Iye adzanditchula ndi kuti inu ndinu Atate wanga, Mulungu wanga, ndi thathwe la chipulumutso changa. Inde ndidzamuyesa mwana wanga woyamba, womveka wa mafumu a padziko lapansi.” (Masalmo 89:26-27). Taonaninso mau amene Yesu adalankhula kwa Maria ankafa: *“Ndikwera kumka kwa Atate wanga, ndi Atate wanu, ndi Mulungu wanga, ndi Mulungu wanu”* (Yohane 20:17).

Pakungowona malembowa tikumbukiradi kuti Yesu anafuna funanso kuti apulumutsidwe ku imfa imene inampeza mthupi la Adamu. Mwaichi, polankhulanso za imfa ndi kuukanso kwa akufa, Petro akuti: *“...ameneyo woperekedwa ndi uphungu umene unayikidwa ndi kudziwikiratu kwa Mulungu, inu mwampachika ndi kumupha ndi manja anu osaweruzika; yemweyo Mulungu anamuukitsa, atamasula zowawa za imfa, mwakuti sikunali koyenera kuti iye agwidwe nayo”* (Machitidwe 2:23-24). Sikudalitu koyenera kuti Khristu akhale mmanda namusunge chifukwa analibe tchimo

popeza ife tidziwa kuti mphotho ya uchimo ndi imfa, komatu Yesu, ngakhale adayesedwa, nafa, sadalekerere kuti tchimo ligwire ntchito mwa Iye. Choncho, kudali kosayenera kuti Iye ngati munthu ochita chilungamo akhale mmanda. Mulungu ali olungama mnjira zake zones ndipo anamuukitsadi. Chifukwa Iye anamvera, nalemekezeka. Yesu adagwiritsira ntchito chiyero kuti awononge mbola ya tchimo ndi chivundi kwa Iye yekha ndi onse amene abatizidwa mdzina lake.

Podziwa kuti Khristu anaukitsidwa kwa akufa, sadzafanso; imfa sidzachitanso ufumu pa Iye. Pakuti pakufa Iye, anafa kuuchimo kamodzi; ndipo pakukhala Iye wamoyo kwa Mulungu ali ndi moyo kwamuyaya. (Aroma 6:9-10).

Adafa pansu pa zonse zimene zimapangitse kuti munthu afe mu uthunthu wa umunthu, koma adaukitsidwa ku moyo wosatha chifukwa sikudali koyenera kuti munthu wosachimwa akhale mmanda:- Khristu amene, mmasiku athupi lake anapereka mapemphero ndi mapembedzero pamodzi ake ndi kulira kwakukuru ndi misozi kwa iye amene akhoza kupulumutsa Iye mu imfa, ndipo anamveka popeza anaopa Mulungu, angakhale anali mwana, anaphunzira kumvera ndi zimene adamva kuwawa nazo; ndipo pamene anayesedwa wamphumphu, anakhalira kwa onse akumvera Iye chifukwa cha chipulumutso chosatha. (AHebri 9:7-9). Simwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe ayi, koma mwa mwazi wa Iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo chiwombolo chosatha. (AHebri 9:12).

Apatu Paulo akuyerekezera kulowa kumalo opatulika kwa wansembe wamkulu ndi kulowa kwa Khristu kumwambamwamba (vs.24). Pamenetu wansembe ankalowa ndi kupereka mwazi wa nyama, zoperekazi zinkalosera (zinali chithunzi) kuchokeredwa cha Mwana wa nkhosa, amene ali Mwana wa Mulungu Mwini. Tikuwona tsopano kuti pachifukwa cha kudzipereka kwake Yesu, adalandira chiombolo chosatha kwa Iye yekha. Mwanjira imeneyi, Khristu adapulumutsidwa ku nsinga ndi chibvundi. Chibvundichi ndizo zofowoka zathu mu uchimo chimene chikuwonetsa poyera kuti ndichomwe chingatilepheretse kupeza chipulumutso mwa Khristu Yesu. Ndipo onani kuti Khristu adathyoleratu cholepheretsacho pa imfa ya pamtanda kwa Iye yekha kuti ife tipeze mpumulo mwa Iye. Kotero,

iyе amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi anaginjetsedwa (AHebri 2:14). Moteronso, ife tilandira “*chiombolo*” mkuzunzika kwa Yesu pamtanda paja.

“Koma Mulungu wa mtendere amene anatipatsa Iye woturuka mwa akufa, ndiye Mbusa wa Mkulu wa nkhosa, amene ndi mwazi wa chipangano chosatha anagonjetsa mphamvu ya imfa, ndiye Ambuye wathu Yesu, choncho, akuyeseni inu opanda chilema mchinthu chiri chonse chabwino, mukachita chifuniro chake nthawi zonse. Motero, chitaninso chomkondweretsa pamaso pa Mulungu mwa Yesuyo, ndipo kwa Iyeyu kukhale ulemerero ku nthawi za nthawi. Amen” (AHebri 13:20-21).

Apatu Paulo akutsimikizira kuti Yesu adaukitsidwa kwa akufa mmwazi wa pangano losatha. Ndipo mwazi umenewu, Khristu adawauza akuphunzira ake kuti: “*Pakuti ichi ndicho mwazi wanga wapangano, wothiridwa chifukwa cha anthu ambiri kuchotsa machimo*” (Mateyu 26:28). Ndimwazi umenewu, umene ukufotokozerwa za moyo wake. Adadzipereka yekha (Mateyu 20:28), kupulumutsa mtundu wa anthu kunsinga za uchimo ndi chivundi ndinso mchikhulupiriro kuti tonse tidze kwa Mulungu mwa Iye.

Pamene Yesu anakhomedwa pamtanda adawonetsa kubvomereza kuti thupi lakelo limene likuyimiranso zilakolako zake, linali lofowoka ngati momwe ife anthu tiliri ndipo izi zinachitika mchifuniro cha Mulungu. Paulo adalembanso kuti: “*Iye adaoneka ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda. Mwa ichinso, Mulungu anamkwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti mdzina la Yesu bondo liri lonse lipindike, la za mmwamba ndi padziko, ndi malilime onse abvomereze kuti Yesu Khristu ali Mbuye nachitira ulemu Mulungu Atate”* (Afilipi 2:8-11). Pakumvera Mulungu mpaka kotsiriza, Iye analemekeza Mulungu Atate wake ndipo moteronso, Atate akewo adakwanitsa zomwe anamutumizira Khristuyo. Ndipo tsopano; “*...Atate inu, lemekezani ine ndi inu nokha ndi ulemelero umene ndinali nawo....*” (Yohane 17:5). Mwaichi, Khristu lero ali kumwamba nakhala kudzanja la manja la Mulungu Atate.

Pochita chifuniro cha mulungu mmoyo wake wonse, ngakhale paka imfa yapamtanda, adatsakula njira kwa onse amene adzabatizidwe mdzina lake, kuti nawonso adzalandire nawo moyo wosatha umene iye adatipezera mkuzunzika. Pamenepatu akupheratu thupi la umunthu limene lidalowerera mmakhalidwe oyipa, nilibweretsa tchimo padziko lapansi. Mchikhulupiriro ndi chowonadi chodabwitsa, timamuona Iye **“amene anasenza machimo athu mwayekha kuti tikafa kumachimo tikhale ndi moyo mchilungamo chake; ameneyo mikwingwirima yake tinachiritsidwa nayo”** (1 Petro 2:24). Chinthunzi thunzi chakumvera kwake, tiyenera kuyamikira pozindikira kuti; **“.....kupyolera mkumvera kwake...anathana ndi imfa, naonetsera poyera moyo ndi chosabvunda mwa uthenga wabwino”** (2 Timoteo 1:10).

9.4 YESU NDIYE AMATIYIMIRA KWA MULUNGU

Tawona kuti nsembe sinali yokwanira kuyeretsa tchimwo koma Yesu ndiye nkhoswe yeniyeni ndipo kuti anayesedwa mzonse ngati ife amene tiri abale ake (AHebri 2:17) **“Adalawa nawo imfa m'malo mwa munthu aliyense”** (AHebri 2:9). Tione kotero, kuti ngati tichimwa tilapa machimo athu, Mulungu atha amatifanantsa ndi Khristu amene adayesedwa ndi tchimo koma komalizira adagonjetsa mayesero onse. Choncho, Mulungu atha kutikhululukira ife machimo athu ngati tingakhala mwa Khristu. Tiyenera kubvala chilungamo cha Khristu ndipo tikatero, Iye adzakhala nkhoswe yathu nthawi zonse. Mulungu akutionetsa chisomo chake ndipo anachita kale ichi potiwonetsera mmalemba ake opezeka m'Baibulo lomwe Buku Lopatulika.

Ngati Yesu akadakhala Mulungu osati munthu ngati ife tomwe, sizikadathekanso kuti Iye akhale otiyimira ngati nkhoswe yathu pakati pa ife ndi Mulungu ayi. Yesu potiyimira, awonetsa chikondi chake paife ndipo izi zikulosera ku machimo athu amene timachita tsiku ndi tsiku koterodi, nkofunika mkhalapakati amene angalumikize ife ndi Mulungu. Kotero, sichinthu chabwino kuti ife

tizikamba za imfa ya Khristu molakwika ngati mmene anthu ena amanenera za Yesu. Maganizo oterewa, amati machimo athu adampereka mngongole yakwa Mulungu imene Iye yekha sakadatha kupereka. Kenaka iwo amati Khristu adapereka ngongoleyi kwa okhulupirira aliyense ndi mwazi wake, umene udakhetsedwa pamtanda. Olalikira wina adanena kuti zidali ngati kuti anthu onse adandanda pakhoma, kuti aomberedwe ndi mdierekezi. Kenaka Yesu adathamanga, ndipo mdierekeziyu adaombera Yesu mmalo mwa ife choncho tiri mfulu.

Sitingawerenge za mabodza ngati awa m'Baibulo. Palitu kutsutsana kwakukulu pakati pa Buku Lopatulika ndi maganizidwe amenewa ndipo kuti ngati Khristu adafa mmalo mwa ife, ndiye kuti ife sitingathe kuchitapo kanthu pa chipulumutso cha moyo wathu chifukwa Yesu adafa akale kufera ife ndipo koteru, sitingafenso. Pakuti tiri mu uthunthu wa thupi la nyama, lochimwa, tiyenera kufa ndithu; chipulumutso ku utchimo ndi imfa zidzaonekera poyera pa chiweruzo (Pamene tidzapatsidwe thupi losafanso monga limene Yesu ali nalo lero lino). Sitingalandire ichi ngakhale kuti Yesu adafa kale koteru, panthawi imene Khristu adafa, anagotilozera njira yeni yeni ya chikondi chimene ife tiyenera kukhala nacho pakati pathu. Imfa ya Yesu idagonjetsa mdierekezi (AHebri 2:14) koma osati mdierekezi kugonjetsa Iye ayi.

Baibulo limatiphunzitsa kuti tingapulumsidwe kupyolera mu imfa ya Khristu ndi kuuka kwa akufa kumene Iye analandira kwa Mulungu osati imfa chabe ayi. Khristu adatifera ife kamodzi. Nkhambakamwa zoti adalowa mmalo mwathu zitanthauza kuti ayenera kufera munthu aliyense payekhapyekha munthuyo osachitapo kanthu chimene sichikugwirizana ndi zimene Baibulo limanena.

Ngati Khristu adapereka ngongole ndi mwazi wake, ndiye kuti zitanthauzanso kuti chipulumutso chathucho, tiyenera kuchilandira popandanso kuchita kanthu kena kalikonse. Pali mfundo yoti chipulumutso ndi mphatso yaulere, imene idza muchifundo ndi chikhululukiro cha Mulungu, nchosamveka bwino ngati timvetsetsa kuti nsembe ya imene iri Khristu, idapereka ngongole yathu mmalo mwa ife. Ikuonetsanso kuti Mulungu amene adakalipa adakondwera atangoWona mwazi wa Yesu. Chenicheni nchakuti ngati ife tirapa mdzina la Yesu amene ali otiyimira pakati paife ndi Mulungu, tiyenera tiziphunzira zimene

Iye anachita kuti athe kugonjetsa tchimo. Ndipo tikatero, Mulungu Atate wake amenenso ali Atate wathu adzamvetsetsa za mabvuto athu chifukwa Khristuyo ali otiyimiradi weniweni. Anthu ambiri amene amati ali mwaa Khristu, amayimba nyimbo zosiyana siyana zimene zimakhala ndi chiphunzitso chonyengachi poyimbira zipangizo zokopa anthu kuti ziphunzitsozo zimveke msanga anthuwo mowakopa chabe mmalo mongofotokozerwa bwino zimene Baibulo limaphunzitsa pa nkhani zambirizi. Tiyenera kupewa zinthu ngati zimenezi. Nchomvetsa chisoni kuti mau oti **“Khristu adatifera ife”** (Aroma 5:8) samamvetsedwa bwino bwino ndi anthu ambiri. Iwo amaganiza kuti mau’wa amatanthauza kuti Khristu adafa mmalo mwathu. Tiona kuti pali mgwirizano weniweni pakati pa Aroma 5; 1 Akorinto 15; (mwachitsanzo Aroma 5:12=[afanana ndi]1 Akorinto 15:21; Aroma 5:22). **“Kristu adatifera ife”** (Aroma 5:8) amagwirizana ndi **“Khristu adafera zochimwa zathu”** (1Akorinto 15:3). Imfa yake idapereka njira yoti kuti ife tikhululukidwe machimo athu, idali mnjira imeneyi yachikhululuko motero, **“Khristu adatifera ife”**. Mau oti **“Kufera ife”** sakutanthauza “mmalo mwa ife” ayi. Khristu adafera zochimwa zathu basi, osati mmalo mwa mwathu ayi. Chifukwa chaichi, Khristu “atha kutipempherera machimo athu (AHebri 7:25) osati kupempha mmalo mwathu ayi. Kapenanso kuti “Ku” amatanthauza mmalo mwa “pa” (AHebri 10:12 ndi Agalatiya 1:4). Chikadakhala kuti Khristu adafa “mmalo mwa ife”, sipakanakhala chifukwa choti ife tisenze mtanda wake. Ndiponso sipangakhale chifukwa chomveka bwino kuti tibatzidwe mu imfa yake ndi mkuuka kwake pofuna kuti tidziwike dzina likhale pa mndandanda wake oti Iye ngati amene adatigonjetsera zonse atiwerengere ndi kutiyerekeza pamodzi ndi ena onse m’Buku lake la moyo. Maganizo oti Iye ndi njira yathu atiwumiriza ife, kuti tibatzidwe muimfa yake ndi mkuuka kwake munjira yoyenda mwa Iye komanso pakuonetsa kuti tidauka naye mu ubatizo. Kuuka kwake kupereka chiyembekezo chaife kuti tidauka chifukwa tiri mwa Khristu amene adaukitsidwa (1Petro 1: 3). Ambuye Yesu adakhala ndi moyo ndi nafa mthupi lathuli mnjira zonse kuti ife timuyandikire komanso kuti titha kumdziwitsitsa Iye mopanda mantha. Pozindikira ichi, tikuona kuti chiphunzitso chotere nchaphindu mmiyoyo yathu. Tidziwa tsopano kuti Khristu adavutika mu Mzimu wake ndipo atha kukhutitsidwa nafe pamene tachita bwino. Tikuonanso kuti pali chotizindikiritsa pamene Ambuye adamuthandiza munthu wina amene lilime lake silinkagwira

bwino ntchito, sankatha kulankhula. Ifenso tikhoza kupindula mwanjira yomweyi popeza tadziwa tsopano kuti Yesu amachiza.

9.5 YESU POTSAGANA NDI LAMULO LA MOSE

Yesu pokhala nsembe yeniyeni yangwiro ya tchimo komanso Iye ngati Wansembe Wamkulu weni weni amene angathe kutikhululukira, atabwera padziko lapansi anachotsa nsembe ya nyama pamene adatifera ife pamtanda paja (AHebri 10:5-14). Nsembe itasinthidwa (kuchokera kwa a Levi ndikukhala mwa Khristu), padayeneranso kusintha lamulo (AHebri 7:12). Khristu *“Wakhala Wansembe osati chifukwa cha lamulo monga makolo anachitira ayi (nthawi imeneyo amuna onse a nyumba ya Levi ankayenera kugwira ntchito ya unsembe), koma pachifukwa cha mphamvu yokhala nayo Iye ndiyo moyo umene sudzaonongedwanso,”*; Moyo umenewu adapatsidwawo nchifukwa cha unsembe Wake wangwiro (AHebri 7:16). Choncho, chidali chofunika kuchotsa lamulo lakale (kunena kuti lamulo la Mose) chifukwa lidali lofowoka ndi lopanda phindu mzinthu zina zokhudza chipulumutso cheni cheni cha Yesu. Chifukwa cha chimenechi, tiwona kuti Yesu anabweretsa chiyembekezo chachikulu pakati pa anthu amene sanali oyenera mpang’ono pomwe kulandira nawo chiyembekezo chimenechi cha chipulumutso (mwa Khristu - AHebri 7:18,19). Apa tikudziwa tsopano kuti mpomveka kuti lamulo la Mose linaunikidwanso ndi nsembe ya Khristu. Kudalira ansembe masiku ano amene ndi anthu wamba kapenanso tinene kuti kupereka nsembe ya nyama Khristu atadzipereka chifukwa chaife kotero sichanzeru, tisowa mtetezi weni weni. Chachikulu, tikhale nacho ife chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu popeza Iye ndiye nsembe yeni yeni yopezekeratu pakati pathu. Palibe munthu adzayesedwa olungama pamaso pa Mulungu ngati sitidziwa Yesu; *“...pakuti wolungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro”* mwa Yesu Khristu (Agalatiya 3:11; Habbakuk 2:4). Tiyenera kumvetsa motero kuti ngati ife tifunitsitsa kukhala olungama pamaso pa Mulungu, sitilungama chifukwa cha malamulo ayi koma

chikhulupirira mwa Yesu Khristu ndi kuchita zonse mchowonadi monga Khristu Iye mwini anachita.

Ngati tikakamira kusunga lamulo la Mose, ndiye kuti tisunge onse bwino bwino mosataya limodzi nkusunga ena ayi. Tikaswa limodzi la malamulowo, tidzatembeledwa: “*..pakuti onse amene atama ntchito za lamulo liwakhalira temberero; pakuti kwalembedwa, wolembe m’Buku la chilamulo, kuzichita izi*” (Agalatiya 3:10). Kufowoka kwa thupi lathu ndiko kutilepheretsa kuti tisunge lamulo la Mose mwangwiro, koma Khristu anamvera mwangwiro lamuloli ndipo ndi Yekhayo anakwanitsa ichi; Mwaichi, Yesu anatisamula mchilamulo chimenechi natipezetsa chipulumutso Iye nakhala mphatso yaulere ya Mulungu mwa Khristu kwa ife, koma osati ifeyo patokha kusunga lamulo ayi. Timawerenga kuti “*..pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita, popeza chinafoka mthupi, Mulungu anatumiza mwana wake wa Iye yekha mchifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha uchimo, natsutsa uchimo mthupi*” (Aroma 8:3). Choncho, “Khristu anatiwombola kutemberero la chilamulo, atakhala temberero lathu” (Agalatiya 3:13). Tiyeni choncho tisawanamize ndikuwatayitsa nthawi anthu powauza kuti ayenera kusunga lamulo la Mose. Tinawona pa Phunziro 3.4 kuti pangano latsopano la mwa Khristu lidalowa mmalo mwa pangano lakale la Mose (AHebri 8:13). Khristu muimfa yake, adafafaniza choyipa chirichonse cholembedwa mu zoyikika zathu, chimene chinali chotsutsana nafe, nachichotsa pakatipo ndi kuchikhomera chimenecho pamtanda; Iye anabvula ukulu ndi ulamuliro wake, nawaonetsera poyera ndikuwagonjetsera. Chifukwa chake, “*..munthu aliyense asakuweruzeni inu mchakudya kapena mkunena tsiku la phwando, kapena tsiku lokhala mwezi, kapena la sabata, ndizo mthunzi wa zirinkudzazo ; koma thupi ndi la Khristu*” (Akolose 2:14-17). Tiwona tsopano kuti izi zikumveka bwino lomwe chifukwa imfa ya Khristu pamtanda paja ndiyo kalilole wathu amene atiwonetsa kuchotsedwa kwa lamulo lija mcholinga chotimasula pa mpanimpani umene unatimangirira ku malamulowo mwachitsanzo, maphwando ndi tsiku la sabata. Monga mwa lamulo, cholinga chake chidali kutitengera ife kwa Khristu. Imfa yake koteru, idakwaniritsa zonse zimene zidali zofunikira mmalamulowa ndipo nkosayeneranso kuwasunga monga iwo ankachitira kale.

Mpingo woyamba kalelo unkaumirizidwa ndi a Yuda kuti azisunga mbali ina ya mamulowo koma tikawerenga mChipangano Chatsopano timamva kawiri kawiri kuti zinthu ngati izi lero lino sikoyenera kutsatira chifukwa sitingakwanitse ayi. Masiku ano iripo mipingo ina imene ikuyesayesa kuphunzitsa anthu kuti azisunga magawo ena a mamulowa. Koma ife tawona kale kuti ngati tiyesa kusunga mbali ina ya lamulo ndicholinga choti tidzapulumutsidwe sitiyenera kusunga mbali imodzi yokha ayi koma malamulo onse ndipo ngati sititero, tidzitemberera tokha (Agalatiya 3:10).

Ena amaganiza kuti Mulungu angawayenereze olungama chifukwa cha ntchito monga kupereka chakhumi motsata lamulo, kubvala korona ndi zina zotero koma nkumachitabe utchimo, motero timayesa kuti tidzapulumutsidwabe ndipo izi zikuchitikadi mmatchalitchi ndi a khristu ambiri lero pakati pathu. Dziwani abale kuti Mulungu akufuna kuti ife tiwonetse ntchito zathu mkuyera. Chipulumutso chagona mchikhulupiriro mwa Khristu Yesu yekha, ichi ndicho chiphunzitso cha Baibulo kuti a khristu onse azitsata.

Ena amatsamira chiphunzitso chawo pa mdulidwe monga mwa lamulo la Mose, **“sungani lamulo”**, Yakobo akutsutsiratu maganizidwe oterewa kwa okhulupirira eni eni. Machitidwe 15:24, Petro adawanena amene ankaphunsitsa zosunga lamulo ngati kuti **“akuyika goli pa makosi a ophunzirawo”** zimene ngakhale iwo kapena makolo sakadazikwanitsa. Koma tikukhulupirira kuti kupyolera mwa chisomo mwa Ambuye Yesu Khristu (Osati kudalira ntchito za lamulo) ife tidzapulumutsidwa (Machitidwe 15:10,11). Mtumwi Paulo yemwe adali mmodzi wa owuziridwa ndi mphamvu ya Mulungu, adabwerezanso mfundoyi **“Munthu sadzayesedwa olungama koma ndi chikhulupiriro cha Khristu, ndipo sintchito za lamulo ayi; pakuti palibe munthu adzayesedwa olunga ndi ntchito za lamulo.....koma mwa (Khristu) onse okhukupirira ayesedwa wolungama mu zonse, zimene simukadatha kukhala olungama ndilamulo la Mose”** (Agalatiya 2:16; 3:11, Machitidwe 13:39).

Chifukwa chosamvetsetsa bwino chiphunzitsochi mchoonadi, ambiri masiku ano amadalira pazinthu zabwino zimene iwo amachitira mpingo motsata lamulo la Mose koma osazindikira chindunji chake cha Baibulo pa zimenezi. Tawona kuti angakhale malembo a m'Buku Lopatulika amanena momveka bwino kuti Khristu

sanalole kusunga zonse za lamuloli mosazindikira ndipo kuti panopa lamuloli nlosayenera chifukwa lidachotsedwa ndi Khristuyo. Motero tsopano, tiwona zina zodziwika mlamulo la Mose zimene a khristu ena akumatsatirabe mpaka pano ngakhale kuti zinthuzo sizikugwirizana ndi pangano latsopano. Anthu ambiri tikulephera kutumikira Mulungu mchowonadi potaya pangano lathu latsopano chifukwa cha zinthu zimene tidakhulupirira kalelo ndipo kuti popeza sitikufuna kuzisiya.

ANSEMBE

A mpingo wa akatorika ndi Angrican amakhulupirira kuti unsembe wa anthu uli woyera koposa china chirichonse mchipembedzo. Akatorika amati Papa ndi ofanana ndi Wansembe Wamkulu wa Ayuda. Iwo amanena izi poganizira kuti Papayu ali pa mzere umodzi ndi Khristu Yesu, kenaka Yesuyo anasiyira Petro, nabwera Paulo ndipo Papa akubwera atapita onsewa. Ife tikuti izi zilibe umboni weni weni m’Baibulo motero, tikudziwa kuti pali **“nkhoswe imodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiyo munthu Khristu Yesu”** (Timoteo 2:5). Nkosayenera choncho, kuti Papa kapena Wansembe akhale nkhoswe yathu panopa popeza ife tikudziwa tsopano kuti ansembe onse kalelo adali pansu pa Chipangano Chakale pamene ife lero tiri m’Chipangano Chatsopano mwa Khristu Yesu. Khristu ndiye Wansembe Wamkulu amene akupereka mapemphero athu kwa Mulungu. Iye ndiye akulumikiza ife ndi Mulungu Atate wathu. Palibe umboni wina uliwonse m’Baibulo kotero, omwe ungatsimikizire kuti maudindo ena amene adalipo nthawi imeneyo anapatsidwa kapena tinene kuti anasiyidwa mmanja mwa anthu ena amene mpaka lero ali m’maudindo akalewo ayi. Koma tiyenera kudziwa kuti Mzimu Woyera udapatsidwa kwa anthu amene anabwera pambuyo pa anthu ngati Petro ndi ena otero osati kwa Papa ayi. Ndipo ngati mwina zimenezi zingakhale zowona, palibe umboni umene ukuwonetsa kuti Papa ndi ansembe ena ndiamene adalandira Mzimu ndi udindo kwa okhulupirira oyambirira kalelo.

Mphatso ya Mzimu Woyera itatha, onse okhulupirira amapeza chithandizo cha mawu omwe ali amphumphu m’Baibulo (Onaninso Phunziro 2.2 ndi 2.4). Choncho onse ali abale mwa Khristu, ndipo kuti tonse okhulupirira ndife

ofanana m'mphamvu pamaso pa Khristu Yesu. Mwaichi, palibenso wina amene ali wamkulu kuposa wina mu udindo pamene pali chikhulupiriro. Onse ali a unsembe watsopano pobatizidwa mwa Khristu, pakuti amaonetsa kuwala kwa Mulungu mdziko lapansi (1Petro 2:9). Adzakhala mafumu ndi ansembe mu Ufumu wa Mulungu pamene Khristu adzakhazikitse ufumuwu panso pano akadzabwera (Chivumbulutso 5:10).

Zomwe akatorika amanena pa ansembe awo “Bambo” (mau oti “papa” amatanthauzanso “bamboo”) zikutsutsana ndi mau a Khristu; **“...musatchula munthu aliyense padziko pano atate; pakuti Atate wanu ali kumwamba”** (Mateyu 23:9). Yesu adachenjezeratu zoti tizipatsana maulemu pa zinthu za uzimu monga momwe achitira akhristu anzathu kwa ansembe awo masiku ano. **“...musamutchule wina Rabi, pakuti mphunzitsi wanu ali mmodzi ndiye Khristu, inu nonse muli abale”** (Mateyu 23:8).

Ngakhalenso mabvalidwe a ansembe, mabishopo ndi olalikira ena ali otengera kwa ansembe anthawi ya Mose ndi ansembe akulu, sizitanthuzira kuti iwo akuchita zolongosoka pamaso Mulungu ayi. Kabvalidwe kameneka masiku amenewo kankalosera makhalidwe angwiro a Khristu kotero lero sityeneranso kutero chifukwa Khristu tsopano anakwaniritsa kale cholinga cha Mulungu. Nzomvetsa chisoni kuti masiku ano anthu ena akutenga ulemerero wa Khristu umene udaonetsedwa mmabvalidwe otere kalelo ncholinga chodzipatsa mipando mdzina la Mulungu ena mpaka amakana za kuwuka kwa Khristu namanenanso kuti Mulungu kulibe.

Akatorika amanenanso kuti Maria ndiye wansembe zimene m'Baibulo sizikupezeka paliponse ayi. Iwo amapemphera kudzera mwa Maria mmalo modzera mwa Yesu Khristu Wansembeyo. Iye mkupemphera kwathu, tiyenera tipempha mmdzina lodabwitsa la Khristu Yesu osati mwa Maria ayi (Yohane 14:13,14; 15:16; 16:23-26). Khristu ndiye Wansembe wathu Wankulu osati Maria ayi. Tikumbukire kuti Yesu adamukanira Maria pamene Maria'yo adamfunsa kuti achitire anthu enawo zinthu zofuna kupeza nazo ulemerero padziko (Yohane 2:2-4). Anthu amabwera kwa Mulungu kudzera mwa Khristu yekha (Yohane 6:44).

CHAKHUMI

Chakhumi ndi chinthu chimene chinkachitika mu lamulo la Mose (Nume 18:2) ndipo kuti kudali koyenera a Yuda kuti apereke chakhumi chimene chinali gawo la khumi la zinthu zimene iwo ankapeza pamtundu uliwonse wa chinthucho. Izi zinkaperekedwa ku unsembe wa ana a Levi. Powona kuti tsopano palibe unsembe umenewu, sikulinso koyenera kuti tizipereka chakhumi kwa akuluampingo kapena a busa ayi. Ndizowona kuti pamene tawona kuti munthu amene wadzipereka kugwira ntchito ya Mulungu ndipo sangathe kuchita china chirichonse chifukwa cha ntchito imeneyi, tiyenera timuthandize koma osati ngati chakhumi ayi. Mulungu mwini wake safuna zopereka zathu powona kuti zonse tilinazozizi nzake (Masalmo 50:8-13). Tikangobwerezanso zomwe Mulungu anatipatsa (1 Mbiri 29:14). Tiwona kuti nkosatheka kuti ife tidzapulumutsidwe chifukwa cha zopereka zinthu zathu monga ngati ndalama ndi zina zotero ayi. Pothokoza pa zomwe Mulungu watipatsa, titha kupereka zaulere koma tisanangopereka chakhumi ife eni wake tisanadzipereke kwa Iye chifukwa amafuna ife tidzipereke kaye osati chakhumi cha ndalama zathu zokha ayi. Paulo adaonetsa chitsanzo pa ichi, ponena zenizeni zimene ankaphunzitsa; ***“Perekani matupi anu ngati nsembe ya moyo, yapadera, yobvomerezedwa kwa Mulungu, imene iri ntchito yoyenera”*** (Aroma 12:1).

NYAMA

Mu lamulo la Mose mogwirizana ndi chikhalidwe cha chi Yuda limanena kuti nyama zina zidali zodetsedwa ndipo izi ndi zimene mipingo ina tsopano lino imanena kuti ziyeneranso kutsatidwa makamaka ngati posadya nyama ya nkhumba. Tizindikire kuti Khristu adathetsa lamuloli pamtanda paja kotero, “..asakuweruzeni aliyense m’nyama, kapena mchakumwa kapena pa tsiku...” (Akolose 2:14-16). Choncho, malamulo a Mose akunena zimenezi kalelo Khristu asanathane nazo koma pano tili m’Chipangano Chatsopano chimene chinatimasula m chilamulo cha Mose pozindikira kuti kale kudalibe chipulumutso mwa amitundu koma kubwera kwa Khristu kunabweretsa chipulumutsochi kwa iwo. Kubwera kwake Khristu ***“zakudya zodetsedwa”*** ndi chilamulo ziyeretsedwa.

Yesu adanenanso kuti palibe chakudya chimene chingadetse munthu mu uzimu koma zonse zochokera mu mtima zikhoza kutero (Marko 7:15-23). Ponenatu izi,

Yesu adati zakudya zonse ziri **“zosadetsedwa”** (Marko 7:19). Petro anawuzidwanso zimenezi (Machitidwe 10:14,15) pamene Paulo adatinso **“..ndadziwa, ndikuona mwa Ambuye wathu Yesu Khristu kuti palibe chodetsedwa pa icho chokha”** (Aroma 14:14). Iye poyambapo adati pokana nyama zimenezi, tikuonetsa kufowoka kwathu mu mzimu. (Aroma 14:2). Ngati ife tidya chakudya chirichonse kotero, **“Mulungu sadzatikana”** (1Akorinto 8:8).

Tiyeni abale tizindikire kuti Khristu anayeretsa zakudya zones pamaso Mulungu ndipo lero achikhulupiriro onse ndi ozindikira choonadi ayenera azilandire ndi chiyamiko. (1 Timoteo 4:3).

9.6 SABATA

Chikhalidwe chinanso chimene chawanda pakati pa akhristu ena amasiku ano ponena za lamulo la Mose nchakuti amatsindika kwambiri pa zosunga sabata. Ena amati nkoyenera kwa mkhristu kuti azisunga tsiku limodzi pa masiku asanu ndi awiri kuti likhale loyenera kumayamika nalo Mulungu. Tsiku limeneri amalitchula kuti la ‘Mulungu’ kapena kuti la ‘sabata’. Choyambirira chimene tiyenera kudziwa nchakuti sabata lidali tsiku lotsiriza la masiku asanu ndi awiri pamene Mulungu adapumula atatha kugwira ntchito yolenga dziko ndi kumwamba mmasiku asanu ndi limodzi (Eksodo 20:10,11).

Tsiku la sabata pokhala tsiku lomaliza la masiku asanu ndi awiri, ndilosayenera kulisunga ngati tsiku la sabata lero chifukwa ndilo limodzi mwa malamulo a Mose amene anakwaniritsidwa ndi Khristu Yesu mChipangano Chatsopano chino. Tsiku la sabata lidali **“Chizindikiro pakati pa Ine (Mulungu) ndi iwo (ana a Israel,) kuti adziwe kuti Ine ndiye Ambuye amene ndidawapatula iwo”** (Ezekiel 20:12). Pachifukwa chaichi, nchosayenera kuti a mitundu (amene sali a Yuda) asunge tsikuli chifukwa linapatulidwa mogwirizana ndi chilamulo cha chi

Yuda; “...*Ambuye akupatsani inu* (Osati anthu onse) *sabata lanu Lopatulika*” (Nehemiya 9:14).

Nzowona kuti Mulungu anadalitsa tsiku la chisanu ndi chiwiri (Genesis 2:3) nalipatula kuti likhale lopatulika pakati pa iwo koma sichikutanthauza kuti sabatayi idzisungidwa mpaka lero chifukwa idali ndi malire ake ndi cholinga chake kalelo. Cholinga cha tsiku limeneri linakwaniritsidwa pamene Khristu anabwera padziko lapansi nagonjetsa mphamvu ya tchimo. Nthawi ina Yesu yemweyo adanena kuti mwana wamwamuna anayenera kulandira mdulidwe pa tsiku la chisanu nchitatu pa umoyo wake (8) ngati wangobadwa kumene. Ngati tsiku loti iye adulidwe ligwa pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, (Sabata), ndiye kuti ntchito ya mdulidweyi sinkayenera kugwiridwa popeza patsikuli, munthu aliyense sankayenera kugwira ntchito ina iriyonse. Ndipo tsopano funso limene linabwera ndilo lakuti, pakati pa lamulo la mdulidwe ndi sabata, ndi lamulo liti limene liyenera kuti lisungidwe, lamdulidwe kapena la sabata? Yesu adati, mdulidwe uyenera kuchitika chifukwa udachokera kwa Abraham, pamene lamulo la sabata ndi limene linabwera pambuyo pake ndipo kuti lamuloli linachokera kwa Mose: “*Mose adakupatsani lamulo la mdulidwe osati poti nlochokera kwa Mose ayi, koma kwa makolo anu*” (kutanthauza za kholo lawo Abrahamu)...ngati lamulo la mdulidwe komanso lamulo losunga sabata onsewa ndi oyenera kusungidwa lero, tidziwe kuti kukhala kobvuta kuwalongosola malamulo’wa chifukwa lero tiripo amitundu ambiri kudzera m’pangano la tsopano la Khristu lomwe linathana kale ndi lamulo la Mose. Lamulo la Mose silikanatilola amitundu kukhala nawo mpangano la chipulumutso. Kotero, zikhoza kutibvuta lerolino kuti tisunge mbali imodzi yokha ya lamulo la Mose lomwe ndi la sabata pamene tikulephera kusunga lamulo la mdulidwe ngakhale kuti malamulo onsewa ndi magawo a malamulo a Mose amene sanatiyenerenze. Mdulidwe udali chizindikiro cha pangano la Mulungu ndi Abraham, pamene tsiku la sabata lidali chizindikiro cha lamulo la Mose (Eksodo 31:17) ndipo Yesu pamalamulo amenewa adaweruzwa kuti pangano latsopano ndi Abraham ndiye lopambana. Paulo nayenso akuchitira umboni pamene akunena moganizira za pangano latsopano loperekedwa kwa Abraham (limene liribe ulamuliro pa lamulo la sabata chifukwa panthawiyi lamuloli linali lisanakhazikitsidwe), ndipo ichi nchinthu chimene sitingawonjezere kapena kuchotserapo koma kuchita monga mwandondomeko imeneyi. Tikhoza kufunsa kuti nchifukwa chiyani

lamulo lidawonjezedwa (Agalatiya 3:15,19)? Ndipo pa funsoli, Paulo akuyankha kuti lidawonjezedwa mongoyembekezera chabe pa chimene chinkayembekezedwa kudza. Ichi nchifukwa cha zobvuta zimene zidalipo panthawiyo koma lero, powona kuti lamulo latsopano palibe amene angawonjezere pamwamba pa malamulowa koteronso, anthu ayenera aphunzitsidwe za uchimo ndikuti athe kumvetsetsa za Khristu mmalo mowumirira kuphunzitsa za chilamulo koma kuti chikhale chiphunzitsa cha mbeu yolonjezedwa ya Abraham pamodzi ndi ife amitundu amene tinasandulika kukhala ana a Abrahamu muuzimu.

Tsopano kuti Khristu anadza, sitirinso pansa pa lamulo. Pachifukwa chakuti Khristu adafa pamtanda, lamulo lidachotsedwa mwakuti tsopano palibe chifukwa chosungira sabata, kapena masiku a chaka monga tsiku la imfa ya Khristu kapena la khristmas (Akolose 2:14-17). Mmasiku akalewo pamene a Khristu ena ankabwerera kuti azisunga mbali zina za lamulo la Mose monga ngati sabata, Paulo akuwachenjeza oterewa kuti akubwezera chikhristu mmbuyo; **“kumfundo zofowoka ndi zosathandiza pamene mufunanso kukhala mu msinga . mkusunga masiku** (Mwachitsanzo lamulo la sabata), **ndi miyezi ndi nyengo ndi zaka** (Kutanthauza maphwando a chiyuda). **Ndiri ndichisoni kuti mukubvutika pa chabe”** (Agalatiya 4:9-11). Apa tiwona kuti nchinthu chobvuta kuti tizisunge lamulo la sabata pofuna kudzipulumutsa: Chifukwa nchakuti; wina awona tsiku lina ngati lofunika kuposa lina (ndiye kuti kufunika mu uzimu); pamene wina awona ngati masiku onse ali ofanana komanso ofunika. Munthu aliyense adziwonere yekha mmaganizo mwake chinthu chimene chingakhale cholondola koma zikhale zogwirizana ndi chowonadi. Onani kuti **“...Iye amene asunga mwa Ambuye; ndi iyenso amene sasunga tsiku, achitanso ichi mwakulemeza Ambuye”** (Aroma 14:5,6).

Nchifukwa chake, tikhoza kuwona kuti sitingawerenge zonedwa ndi okhulupirira oyamba aja kuti ankasunga lamulo la sabata. Mmalo mwake, timamva kuti anakumana pa tsiku lililonse loyamba la masiku asanu ndi limodzi mwachizolowezi chawo ndiye kunenanso kuti la mulungu lililonse (Sunday): **“...Patsiku loyamba la sabata, pamene ophunzira anakumana kudya mgonera...”** (Machitidwe 20:7). Ichi nchimene ophunzirawa anakachita kulikonse monganso mmene Paulo adawalangizira otsata Khristu Yesu a ku

Akorinto kuti; ***“aliyense azisunga monga wapindulira patsiku loyamba la sabata”*** (1 Akorinto 16:2), kutanthauza kuti azisonkhana onse patsikulo. Okhulupirira onse kotero, ayenera kutchedwa ***“ansembe”*** (1 Petro 2:9) amene sayeneranso kusunga sabata (Mateyu 12:5) koma kugwira ntchito yawo mmasiku onse ndi nthawi zonse osapuma monga mwa pangano latsopano la Khristu.

Ngati tifuna kusunga lamulo la sabata motero, tiyeni tizisunga lamuloli mwandondomeko yake ya Mose komanso tiyenera kusunga magawo onse a malamulo a Mosewo; tawona kale kuti sichoyenera kwa munthu kusunga lamulo la Mose mbali imodzi yokha; kotero tisadzitengere temberero (Agalatiya 3:10; Yakobo 2:10). Tikhoza kulandira chipulumutso ngati tisunga moyenera lamulo la Khristu osati lamulo limodzi lokha la Mose ayi. Ana a Israeli sankalodwa kuchita ntchito ina iriyonse pa tsiku la sabata. ***“Aliyense amene agwira ntchito patsikuli adzaphedwa. Adalamulidwanso kuti, musamasonkhe moto mnyumba zanu pa tsiku la sabata”*** Iwo ankaletsedwanso angakhale kuphika zakudya zawo patsikuli (Eksodo 35:2,3; 16:23). Mwachitsanzo, munthu wina ankatolera nkhu ni pa tsiku la sabata, mwina ncholinga chakuti akasonkhe moto, iye adaphedwa chifukwa anaswa lamulo la sabata. Tikawerenganso pa Numeri 15:32-36 tikhoza kuwona tokha zimenezi; ngakhale ziri choncho, tidziwe kuti lero lino palibe amene amaphedwa chifukwa chogwira ntchito pa tsiku la sabata angakhale anthu amene amalimbikira kulalikira za tsiku la sabata.

Mipingo imene imasunga tsiku la sabata lero kotero, iyeneranso kuti izipha anthu amene amaswa lamulo la sabatali powalanga ngati momwe zinkachitikira mmasiku amenewo. Iwo aziwonetsetsa kuti pasamakhale kuphika kulikonse patsikuli. Azingokhala nkumapemphera ndi kulalikira mawu a Mulungu basi. Komanso iwo sayenera kuyenda pogwiritsa ntchito galimoto ndi zina zotero komanso kugwira ntchito ya mu ofesi kumene monga mwa malamulo Mose anenera. Mukhoza kuwona kuti aYuda a masiku ano amene amachita zoyenera mu uzimu akamayenda kulikonse kumene iwo apita, amanyamuliratu zakudya zawo zophikaphika pa maulendo awo onse potsata lamuloli. Komatu chomvetsa chisoni nchakuti a “khristu” a masiku ano amalephereratu kutsatira malamulo amenewa.

Ngakhale amene akuphunzitsabe za sabata amati kusunga sabatali chidali chimodzi cha malamulo khumi amene Mose adalandira pa phiri la Sinai lija, ndikuti, angakhale lamulo la Mose lidathetsedwa ndi Khristu, nkoyenera kwa iwo kusungabe malamulo khumiwo ndipo lamulo la sabata ndi limodzi la malamulo amenewa. Makamaka a mpingo wa Seventh Day Adventist ndiamene amakonda kunena kuti pali kusiyana pakati pa lamulo la makhalidwe omwe ali pa malamulo khumi aja, *“lamulo la Mulungu”* ndi lamulo la zochitika (*ceremonial law*), *“lamulo la Mose”* limenenso amakhulupirira kuti lidathetsedwa ndi ntchito ya Khristu. Tikhoza kuwona kuti palibe kusiyana mmalemba Oyera pakati pa ‘malamulo a Mose’ ndi ‘malamulo a Mulungu’. Baibulo limagwiritsa ntchito ‘lamulo la Mose’ ndi ‘lamulo la Mulungu’ mofanana (Numenti 31:21; Yoswa 23:6; 2 Mbiri 31:3)

“Mulungu anakufotokozerani (Israeli) m’Chipangano chake, chimene akulamulirani kuchichita, ndiwo mau khumi; nawalemba pa magome awiri” (Deuteronomu 4:13). Tikumbukenso kuti pangano limeneri lagona pa malamulo khumi amene adapangidwa pakati pa Mulungu ndi a Israel, osati amitundu amasiku ano ayi. Mose adakwera kuphiri la Horebu kukalandira miyala imene Mulungu adalemba natchedwa malamulo khumi. Kenaka Mose adathirapo ndemanga pa malamulowo, Ambuye Mulungu Atate wathu adalonjezana pangano ndi ife ku Horebu (Deuteronomu 5:2) kupyolera m’malamulo khumi aja.

Panthawi imeneyi, Mulungu ***“adalemba pa miyala mau a chipangano m’malamulo khumiwo”*** (Eksodo 34:28). Pangano limeneli lidali lokhudzana ndi lamulo lotchedwa lamulo la zochitika (*ceremonial law*) (Eksodo 34:27). Ngati tikuti tiyenera kusunga pangano la m’malamulo khumi, tiyeneranso kusunga zonse za mmalamulowa, chifukwatu ndi mbali imodzi ya mpanganolo. Komatu tikawonetsetsa, nkovuta kuchita zonsezi monga mwa malembo.

“Mudalibe chirichonse m’likasa koma miyala iwiri basi, imene Mose adaikamo ku Horebu...likasa mmene mudali pangano la Ambuye” (1Mafumu 8:9,21). Pamiyalapa, mpamene padali malamulo khumi aja ndipo ili ndilo lidali pangano ndi Mulungu.

AHebri 9:4 akunena za **“Miyala ya pangano omwe ndiwo malamulo khumi adalembedwa pa miyala nakhala ‘Pangano’ lakale”**.

Paulo akunenanso za panganoli ngati kuti **“.....wolembedwa ndi wolochedwa mmiyala”**. Iyetu akupitirira kunena unali **“utumiki wa imfa...umene unachotsedwa”** (2 Akorinto 3:7-11). Panganoli motero likugwirizana ndi malamulo khumi limene silingapereke chipulumutso pokhapokha ngati ife tichita zonse mwa Khristu. Yesu Khristu ndi amene **“..adafafaniza zonse zimene zidalembedwa za ife zomwenso zidali zotsutsana nafe”** (Akolose 2:14) izi nzimene zikutitsimikizira kuti nzolembedwa monga mwa malamulo khumi amene anali pa miyala paja. Chimodzimidzinsu Paulo akuti **“Lamulo pokhala la kufa.....mchilembo chakale”** (Aroma 7:6); akunenanso za zimene zinalembedwazo.

Lamulo limodzi mwa malamulo khumi likunenedwanso kuti ndilo “lamulo”, makamaka tikawerenga pa (Aroma7:8). Chilamulo chimati usasirire. Ndipo mavesi ena otsatirawo tikawona pa Aroma 7:1-7 amatsindiza za mmene ‘lamuloli’ lidathetsedwera ndi imfa ya Khristu pa mtanda paja: Chilamulo kotero, chikuneneratu za malamulo khumi.

Mwaichi, timvetsa bwino kuti Chipangano Chakale chimanena zamau oti ‘lamulo’ mophatikizapo malamulo khumi. Monga tanena kuti popeza malamulo a Mose adachotsedwa ndi lamulo latsopano la Khristu, malamulo khumiwa ndiye kuti adachotsedwanso. Choncho, malamulo asanu ndi anai(a) adawabvomerezana mu Mzimu mwa Chipangano Chatsopanochi. Malamulo 3,5,6,7,8 ndi 9 tikhoza kuwapeza m’Buku la Timoteo ndipo Malamulo 1, 2 ndi 10 la 1 Akorinto 5. Komatu palibe pena pali ponse m’Chipangano Chatsopano pamene tingapeze lamulo loti tisunge sabata.

Taananitu mndandanda uli mmunsiwu umene ukutiwonetsa mwadule momwe malamulowa adabvomerezedwera mChipangano Chatsopano:-

Lamulo

1 _____ Aefeso 4:6; 1Yohane 5:21, Mateyo 4:10

2 _____ 1 Akorinto 10:14; Aroma 1:25

Mavesi

- 3 _____ Yakobo 5:12; Mateyu 5:34,35
 4 _____ Palibe
 5 _____ Aefeso 6:1,2; Akolose 3:20
 6 _____ Yohan 3:15; Mateyu 5:21,22
 7 _____ Aheberi 13:4; Mateyu 5:27,28
 8 _____ Aroma 2:21; Aefeso 4:28
 9 _____ Akolose 3:9; Aefeso 4:25; 2Timoteo 3:3
 10 _____ Aefeso 5:3; Akolose 3:5.

Ambuye Yesu akutiwitana ife ngati tifunitsitsa chipulumutso mwa Iye ndipo tibvomereze kulandira “mpumulo” umene Khristu akutiwitana (Mateyu 11:28). Yesu adagwiritsa ntchito mau a chiGreek ponena za mpumulo wa tsiku la chisanu ndi chiwiri. Yesu kotero, adapereka moyo woyenera wochitika pa sabata, umene ndi mpumulo unaperekedwa kwa ife kuti tichotse kusakhulupirira kwathu pa ntchito zathu (Aheberi 4:3,10). Choncho, ndichinthu chopanda phindu kuti tikapumule mosazindikira bwino tsiku limodzi lokha pamasiku asanu ndi awiri pamene tikukhala moyo wathu mu Mzimu wa mpumulo (sabata) tsiku ndi tsiku mphindi iriyonse ya moyo wathu pamene tikusachita bwino.

MPATUKO 28: KORONA (MTANDA)

Anthu ambiri amakhulupirira kuti Yesu Khristu adaphedwa pamtanda; Tikawona m’chi Greek, mau oti *‘stauros’* amene amatanthauzira kuti *‘mtanda’* m’Baibulo, tiona kuti liwuli limakamba za umene unali weni weni ‘mtengo oyikidwa’. Chizindikiro chamtanda chikuwoneka kuti chiri ndi maziko achikunjamalingana ndi mbiri yakale. Nkoyenera kuti Khristu adafa ndi manja ake pamwamba pamutu wake osati manja otambasulidwa ngati mmene chithunzi cha mtanda chimawonetsera ayi. Kotero, angakhale kuti manja ake akuwonetsedwa kuti anatambasulidwa kumwamba m’chizindikiro choti ndiwo malonjezano a Mulungu kwaife amene akwaniritsidwa ndikubwera kwake, (Ezekieli 20:5,6,15; 36:7; 47:14) komanso kuyimira mkupemphera kosalekeza, (Maliro 2:19; 1 Timoteo 2:8; 2 Mbiri 6:12,13; Masalimo 28:2) sizitanthawuza

kuti Yesu anachita ichi. Monga m'mene Khristu anawonetsa pamtanda paja, (AHebri 5:7) Yesu akuyimira mkuwa imene idakwezedwera pamtanda paja ndipo momwemonso Mwana Wamunthu adayenera kukwezedwa; nakwaniritsa ulosi wa aneneri pamtanda wa mtengo pamene Iye anakhomedwapo (Yohane 3:14).

A mpingo wa a katorika amadzipereka kwambiri pa ntchito ya mtanda ndipo mpaka amakhulupirira kuti paliponse pamene iwo ayenda ayenera kumabvala korona umene umayimira mtanda. Izitu sikuti zili zidalembedwa penapaliponse m'Baibulo ayi; Iwo chimakhala ngati chizindikiro chawo chabe chimene chimawatsimikizira chipulumutso chawo ndikutinso kuwonetsera kwawo kuti Mulungu ali nawo nthawi zonse. Anthu ena akhala akuganizira kuti akamabvala kawiri kawiri koronayu kapena kuchita chizindikiro cha mwambo wa mtanda ndiye kuti Mulungu ali ndi iwo. Izitu ndizinthu zopanda phindu pa moyo wathu wa chkhristu. Tiyenera kudziwa kuti mphamvu yeni yeni ya mtanda ntchito pamene ife tidzifananitsa mzochita zathu muimfa ya Khristu Yesu ndi khulupirira mwaife, ndipo poyambirira tiyenera kubatidzidwa. Nchapafupitu kukwaniritsa chizindikiro cha mtanda koma osakhulupirira ndi kubatizidwa.

Ndi chinthu chosakayikitsa kuti korona (mtanda) ndi chizindikiro chimene anthu a kunja ankatsata malingana ndi mbiri yakale ndipo kuti chakhala chikuchitika kalelo angakhale pamene Khristu anali asanabadwe. Ichitu nchikunja chenicheni monganso mtengo wa chikondwerero cha khristimas, zimene tsopano zalowetsedwa mu chikhristu ndi m'mpingo tsopano lino.

MPATUKO 29: KODI YESU ANABADWA PA 25 DECEMBER?

Chinthu china chimene anthu sangathe kufotokozerwa bwino lomwe ndicho tsiku lemene Yesu adabadwa. Abusa amene ankaweta nkhoa kutali panthawi imene Khristu anabadwa tikamawerenga m'Baibulo (Luka 2:8); timamva kuti idali nthawi ya khristimas, nthawi iyi ndiyomwe msipu umakhala ponseponse kumalo

kumeneku mdziko la Israel. Nthawi zambiri manyuzipepala aku Israel monga ngati Jerusalem Post ndi ena, akhala akulemba momwe chisanu chakhala chikubvutitsira m'Yerusalemu pa nthawi ya mwezi wa December. Tikatengera pamenepa, Khristu ayenera kuti adabadwa miyezi yozizirayo imene iri cha mu September mpaka mwina October. Kotero, monga tikudziwa kuti December 25 lidali tsiku la chikunja limene ankachita maphwando awo anthu amenewa chikhristu chisanadziwike mbali imeneyi, sizingakhale zowona kuti Yesu anabadwa tsiku limeneri. Tsikuli anangolisandutsa kuchokera ku chikunja nkulikhazika kukhala tsiku lokumbukira kubadwa kwa khristu pofuna kuti chikhwalidwe chawo chachikunjacho chisawatalikire.

Tikawerenga m'Buku la Machitidwe a Atumwi, timamva momwe akhristu enieni adazunzidwira ndi anthu a chikunja chifukwa cha chikhulupiriro chawo mwa Yesu. Nthawi ndi nthawi Atumwiwa akhala akutichenjeza kuti chifukwa chaichi, a khristu ena adzatengeranso zikhulupiriro zachikunjazi ncholinga chopembedza nawo zosayenera zomwe ziridi zinthu zachikoka pakati pawo. Mwachitsanzo, tikawerenga Machitidwe 20:30; 1 Yohane 2:18; 2 Atesalonika 2:3; 2 Petro 2:1-3) tikhoza kuwona tokha zonsezi. Ngati ife tingatengeranso chikhulupiriro cha tsiku la 25 December ndiye kuti tiri mgulu limeneli. Mtengo wa khristimas ndi zina zotere, nzimene zinkachitika pa tsiku limeneli la December 25 zomwe zidali zolemekeza chikunja. Ngati a khristu, siyenera kutsatira izi.

Nchoyenera tsopano kuti a khristu enieni asamatengepo mbali pa zikondwerero zimene zikuchokera kuchikunja monga kubadwa kwa Khristu pa tsiku la December 25. Choyenera kuchita ndicho kukhulupirira chipulumutso chenicheni pa chiphunzitso cha chowonadi cheni cheni cha Mau a Mulungu.

PHUNZIRO 9: MAFUNSO

1. Nchifukwa ninji imfa ya Yesu Khristu, ikusiyana ndi imfa ya munthu wina aliynse ndipo kuti ndiyofunikira kwambiri pa chipulumutso chathu?

2. Ndi chifukwa chiyani nsembe za nyama m'lamulo la Mose sizidali zokwanira kuchotsa tchimo?
3. Kodi Yesu adali myimiriri kapena mlowa malo wa anthu pamene adafa pamtanda paja?
4. Paziganizo izi, ndi ziganizo ziti zimene ziri zolondola
 - (a) Khristu adafa mmalo mwaife
 - (b) Khristu adayimira ife, choncho Mulungu akhoza kutikhululukira mwa Iye.
 - (c) Khristu adali ngati ife koma sikuti akutiyimirira mmachimo athu.
 - (d) Imfa ya Yesu itanthawuza kuti Mulungu sadzasunga munthu aliyense amene ali woipa chifukwa cha tchimo.
5. Kodi Khristu adapindulapo ndi imfa yake?
6. Pamene Khristu adafa pa mtanda paja, kodi
 - (a) Adathetsa malamulo ena ang'ono a m'malamulo a Mose kupatula malamulo khumi aja
 - (b) Adathetsa malamulo onse a Mose kuphatikizapo malamulo khumi aja
 - (c) Adathetsa lamulo la Mose koma maphwando a a Yuda ayi.
 - (d) Palibe chimene adachitapo pa lamulo la Mose?
7. Kodi tiyenera kusunga tsiku la sabata ngati kale tsopano?
8. Perekani zifukwa zake za yankho limene mwapereka pa funso la nambala 7.

PHUNZIRO 10
KUBATIZIDWA MWA YESU

10.1 KUFUNIKA KWA KUKULU KWA UBATIZO

Kwa zimene taphunzira ku mbuyoku takhala tikufotokoza za kufunika kwakulu kwa ubatizo ndi chinthu chimodzi chimene munthu amachita pomvera uthenga wabwino Aheberi 6V2 akunenetsanso zoti ubatizo Ndi chiphunzitso cha pa phata pa ziphunzitso zina zimene ziripo. Tikunena tsopano chifukwatu ubatizo weniweni umachitika ngati munthu walandira chiphunzitso choonadi chimene chiri mu uthenga wabwino;Tsopano tatha kuphunzira choonadichi, ngati mufuna kuti khaledi khuzidwa ndi chiyembekezo chenicheni chimene Baibulo lipereka mwa Yesu Kristu,ndiyetu ndi ubatizo umene ungatitha ndize.

“Chipulumutso ncha ayuda” (yohane 4v22) mu chifukwa chakuti malonjezano amenewo ngati tingakhale mu mbeu yake, pobatizidwa kwa kristu (Agalatiya 3v22-29). Poteropo chimene chingakhale choona kwa yesu kristu chikhalanso choona kwa ife.Zakariya adaona za ulosi okhuzana ndi mbeu ya Abraham ndi Davide ngati akhudza okhulupira onse (Luka 1v73,74).Popanda ubatizo ndiye kuti tiri kunja kwa malonjezano ndi mulungu.Chimo sichinthu chokhacho chingatirepheretse chipulumutso tiyenera kukhala m’malonjezano a ubalenso, kuti tivale chilungamo cha kristu.Ndichifukwa chake petro adati ‘lapani ndi kubatizidwa’ kuti mulandire chikhulukiro.Monga momwe ambiriabatizidwa mwa kristu ali mwa iye ndipo ali ndi malonjezano a chipulumutso amene adapangidwa kwa Abrahamu ndi ndi kwa iwo(Agalatiya 3v27) Ngati tigawana mu imfa ya kristu ndi kuuka kwa kupyolera mu ubatizo, ndiye kuti tsopano zatheka’tidzafananitsidwanso mu kuuka kwake-tidzakhalsanso ndi moyo ndi iye (Aroma 6v5,8).

Yesu adalamula omutsatira ake kuti”pitani mu dziko lonse, ndipo mukalalikire uthenga wabwino (amene muli malonjezano a mwa Abrahamu (Agalatiya 3v8) kwa mitundu yose.Amene akhulupirira ndi kubatizidwa adzapulumutsidwa” (Marko 16v16).Pomvetsetsa bwinobwino mau oti “ndi akutiwululira kuti chikhulupiro chokha mu uthenga wabwino sungatipulumutse ayi; zimene zikutanthauza kuti chikulupiliro chokha mu uthenga wabwino sungatipulumutse ayi zimene zikutanthauza kuti ubatizo sichinthu chogonjetsera mu umoyo wa kristu koma chofunika kwambiri kuti tipumutsidwe sikutinso ubatizo okha ndiye ungatipulumutse ayi komanso zitsatane ndi omvera mau a

mulungu. Yesu adanena motsindika “indetu indetu ndinena kwa inu ngati munthu sabadwa mwa madzindi mu mzimu,sadzalowa mu ufumu wa mulungu “(Yohane 3v5).

Kubadwaku “mwa (chigiriki kuvuuka) madzi “zikutanthauza munthu kuvuuka m’madzi aubatizo kenaka ayenera kubadwa mwa mzimu.Ichitu choti chipitirirebe; kubadwa kachiwiri ndi mau a mulungu” (1 petro1v23). Pamene tikupitirira kumva ndi kuvomereza mau a uzimu tikhala obadwa mu mzimu(onaninso phunziro2.2).

Tiri obatizidwa mwa khristu “(Agalatiya 3v27) mu mdzina lake ndi lake ndi Atate (machitidwe 19v5,8v16, Mateyu 28v19) Timvetsetse apa timabatizidwa mwa kristu osati mwa khilisitafediya kapena mpingo wina ulionse .Tikabatizidwa timaasanduka anthu otchulidwa ndi dzina la yaweh monga ngati momwe israel adachulidwira(2 Mbiri7v14). Kawirikawiri mulungu adachenjeza kuti a Israel adachulidwa ndi dzina lake adayenera kuonetsa udindo mau moyenera ngati mboni zake padziko.Ndichimodzimidzi ndi ife amene tabatizidwa mu dzina lake,popanda ubatizo ndiye kuti sitiri mwa kristu’,choncho ndiyekutisitidavalentchitoyakeyachipulumutso(machitidwe 4V 12) .Petro akupereka fanizo lake pa mfundoyi .Akufananitsa chombo cha Noah ndi Kristu,akuti chombo chidapulumutsa Noah ndi banja lake ku chiweruzo chimene chidabwera pa ochimwa, chimodzimidzinsu kubatizidwa mwa Kristu kudzapulumutsa okhulupirira ku imfa yosatha (1Petro 3V21).Monga momwe Noah adalowera mu chombo muja zikufanananso ndi. Ife kulowa mwa Kristu kupyolera mu ubatizo .Monga momwe Noah adalowera mu chombo muja zikufanananso ndi ife kulowa mwa Kristu kupyolera mu ubatizo. Onse amene adali kunja kwa chombo adaonongedwa Ndi chigumula ; kukhala pafupi ndi chombo kapena kukhala bwenzi wa Noah Sizidali ndi phindu koma kulowa mkati mwa kristu kupyolera mu ubatizo.

Onse amene adali kunja kwa chombo adaonongedwa ndi chigumula, kukhalapafupi ndi chombo kapena kukhala bwenzi wa Noah sizidali ndi phindu koma kulowa mkati mwachombo.Njira yokhayo imene idayererera tingapulumutsidwe ndi idali ndipo iri yoti tikhale mwa kristu/chombo.Umboni onse ulipo kuti tikubweranso kachiwiri kumene chigumula chidafananitsidwa (Luka 17v26,27),kuli pafupi nafe (onani ndemanga ya 3) kulowa mwa kristu/mu chombo nkofunika kuchita msanga.Mautu amene munthu anganene anganene

akhoza kulephera kuti afotokoze kufunika kolowa mwa kristu/mu chombo,koma zomwe tikumva mmene Nowa adalowera mkwamphamvu.

Akristu oyambirira adamvera lamulo la kristu kuyenda m'malo osiyanasiyana pa dziko lapansi kukalalikira uthenga wabwino ndi kubatiza, izi timawerenga pomva mmene anthu ankatizidwira ankangovomereza uthenga wabwino (mwachitsanso Machitidwe 8v12,36,39:9v18,10v47,16v15)kutsindikaku tikhoza kumvetsa ngati ife tizindikiradi kuti popanda ubatizo palibe chiyembekezo chenicheni ngakhale tingaphunzire za uthenga wabwino, chifukwa ubatizo uli ofunikira kuti ife tidutse njira yopita kuchipulumutso. Tikamawerenga malembotimamva mmene anthu ena ankachdwetsera kubatiza anthu komatiyeni tiyesetse kuti izi zisatichitikire pothandizidwandi mulungu.Mdino wa filipi adadzizidimuka ndi chivomerezi chimene chidononga malinga andende ndipo akaidi adali ndi ufulu onse kuthawa-chinthu chimene chikadampangitsa kuti aphedwe.Chikhulupiriro chake mu uthenga wabwino chidaonekeradi tssopano, mwakuti “ola lomwelo lausiku adabatizidwa... nthawiyomweyo” (Machitidwe 16v33) Ngati wina wake achedwa kuti abatizidwe ndiyekha.Padali chivomerezi choopsa kuposa zina ku Greece pa zaka zapita zoposa zikwi zitatu,pamene akaidi onse adaona mbiri imene idali isadachitikenso pamene ndende idatsatuka yokha ndipo mdindo adali pa ngozi kuti akadatha kuphedwa chifukwa choti walephera ntchito,ndipotu adaonetsetsa choti akadayenera kuchita mmoyo wake ndipo chidali choti apeze njira yoti adzapeze moyo wosatha. Atangotero adagonjetsa mavuto amene adamuzungulira (monga chivomerezi),zipsinjo za pa ntchito zatsiku ndi tsiku ndinso kunjenjemera kumene adali nako-chifukwa cha ubatizo zonse zidatha.Ambiri amene akuchedwa kuti abatizidwe akhoza kutengerapo phunziro kwa munthuyu.Posankha njira imeneyi ya chikhulupiriro ndi chitsimikizo choti adali kale ndi chiphunzitso cha uthenga wabwino, podziwa kuti chikhulupiriro chenicheni chimadza pomva mau a mulungu (Aroma10v17/Machitidwe 17v11).

Pa machitidwe16v14,15 timawerenga kuti Lidia adatsatira zomwe paulo adalankhula.Ndipo adabatizidwa.... “zimene zikutionetseratu kuti aliyense amene omva ndi kukhulupirira uthenga wabwino adzabatizidwa ndipo ubatizo akuonetseratu kuti ndiye njira yokhayo yovomerezerakuti munthu wamvetsetsa za ulaliki wa uthenga wabwino.Ntchito zabwino sizikukwanira pazokha tiyenera

kuti tibatizidwenso. Koneliyo adali munthu odzipereka ndi oopa mulungu.... amene ankapereka ku wanthu zinthu zambiri, ndi kupemphera kwa mulungu nthawi zonse: komatu izi sidali zokwanira, adaonetsedwa zoyenera kuchita zomwe adali asanachite kodayenera kuti abatizidwe (Machitidwe 10v2,6).

Machitidwe 8v26-40 tikuwerenga kuti munthu wa ku Ethiopia ankawerenga Baibulo pamene adali atakwera pa gareta wake mu mchipululu. Adakumana ndi filipo, amene adamufotokozerera bwino bwino za uthenga wabwino komanso za kufunika kwake kwa ubatizo. Ponggoganiza chabe munthu zidali Zosatheka kuti munthu angamvere lamulo loti abatizidwe mu mchipululu moti Mudalibe madzi, kotero mulungu sakadapereka lamulo loti akudziwa kuti ena Sakadatha kulimvera. Pamene ankapitirira ulendo wawo, adafika pamalo pena Pamene padali madzi,” kutanthauza kuti padali kadziwe, pamene ubatizo udayenera kuchitikira (Machitidwe 8V36). Izitu zikusutsa zimene anthu ena amanena kuti ubatizo omira pamadzi un kayenera kuchitikira pamalo pomwe pali madzi okwanira. Mulungu amapereka zinthu zoyenera kuti malamulo ake atheke kutsatidwa.

Paulo mtumwi adalandira masomphenya ochokera kwa Kristu amene adamukhudza kwambiri mwakuti sakadachitira mwina koma ‘adangonyamukanthawi yomweyo ndikubatizidwa “(Machitidwe 9V18). Apanso mwina tikhoza kuganiza kuti nayenso ankaganizira zoti azengereze poonaso za zimene ankachita ku moyo wakale wa chi Yuda. Koma chifukwa cha zomwe adazona adazipereka kuti abatizidwe ndiponso kunena poyera kuti waleka umoyo wake wakale. Kenaka adaonetsa phindu la kusankha kumene adsankhaku kuti abatizidwe .” Zinthu “Zinthu zimene zidali zaphindu kwa ine, zimene ankaona ngati “zaphindu” kwa iye), ndi kuziona ngati ndowe, kuti ndipeze Kristu.....poyiwala zonse zakale (zimene ankachita ku moyo wakale wa chi Yuda), ndi kufika ku zinthu zatsopano, ndi kupereka chizindikiro cha mphotho (Afilipi 3V7,8,13,14).

Izitu ndi zimene ochita mpikisano othamanga angachite kuti apambane. Zoterezi ndi zimene tiyenera kuchita kuti maganizo athu ndi zochitika zathu ziwongolere miyoyo yathu pa umoyo wathu titabatizidwa. Tiyenera kumvetsetsa apa kuti ubatizo ndicho chiyambi cha mpingo ndi zikhulupiriro, kapenanso kuti

zitipangitse kuti tsopano tamasulidwa kuti tikhoza kuchita chirichonse pa umoyo wathu wa chi Kristu. Ubatizo umatiphatikiza ife kuti nthawi potha nzeru, Paulo adati: “Sindidali osamvera ku masomphenya “(Machitidwe 26V19). Monga momwe zidaliri kwa Paulo, sizirinso chimodzimodzi kwa iwo amene adbatizidwa moyenera: Ubatizo ndi chinthu cha mtengo wa patali chimene munthu ngati wachichita ndiye kuti wachita chinthu cha nzeru. Kulapa kuli koyenera ndithu, Paulo akuti (2Akorinto 7V10). Pa zonse zimene munthu achita pa zomwe waganiza kuti achite chanzeru pobatizidwa. Pa zonse zimene munthu achita pa Zomwe waganizira kuti achite chanzerutu ndi ubatizo .Funso lanzeru kwambiri loti tiyankhe ndi lakuti: ‘Ndi chifukwa chiyani ndilephera kubatizidwa?’

Kodi YENI YIMENE TIYENERA KUTSATA POBATIZIDWA NDI ITI?

Palitu maganizo osochoretsedwa amene anthu amatsata , makamaka pobatiza wana, ena amangodontheza madzi pamutu (amati kumuyeretsa). Izitu sizimene Baibulo limaphunzitsa ayi.

Mau a Chigiriki ‘Baptizo’ amene kumasulira kwake ndi “baptize” mu chingerezi. Mauwa siatanthauza kudontheza ayi: amatanthauza kusamba thupi Lonse pamene wamizidwa pamadzi (Onani mmene concordance ya Robert Young ndi James Strong ikufotokozerana).

Mauwa amagwiritsidwa nchito mu chi Giriki pa sitima za pamadzi zimene amati zimira pa madzi kapenanso ngatichidebe cha madzi chamira pa chitsime. Nthawi zinanso amagwiritsidwa nchito ponena za nsalu ngati yasintha mtundu pamene yamizidwa mu makhwala pachingerezi amati (dye). Kuti tisinthe mtundu wansalu, tiyenera kuti nsaluyo imizidwiretu yonse, osati kungowaza ayi. Chifukwa tikawaza ingooneka kuti iri ndi madontho.

Pa Yohan 13V26 adagwiritsa nchito mau a chigiriki ‘bapto’ kunena za mmene Ambuye adanyikira mkate mu vinyo. Kutitu titsimikiziredi kuti ubatizo weniweni ndi kumizidwa tikhoza kuwerenga mavesi awa:-

Ndipo Yohane anali nkubatizidwa m’Ainoni pafupi pa Salemu, chifukwa panali madzi ambiri pamenepo: ndipo analikufikapo anthu, nali kubatizidwa .

“(Yohan 3V23). Umboni ulipo apa kuti ubatizo weniweni umafunika madzi ambiri; zikadakhala kuti ankangodontheza pamutu, ndowa imodzi yamadzi ikadatha kukwanira miyandamiyanda ya wanthu. Anthu adabwera kumtsinje wa Yordan osati kuti nabatizidwa atatenga madzi mu botolo.

*Yesu naye, adabatizidwa ndi Yohan mu mtsinje wa Yordan - mu Yordan (Marko 1V9).

“Yesu, atangobatizidwa, adavuwuka mmadzi”(Mateyu 3V13-16).Ubatizo wake udali omizidwa adavuwuka mmadzi atabatizidwa. Pa zifukwa zimene Yesu adabatizidwira,chimodzi cha icho chidali chotipatsa ife chitsanzo chake cha ubatizo womizidwa.

*Chimodzimodzinsu, Filipi ndi mdindo “adtsikira onse awiri kumadzi...ndipo adabatizidwa.Ndipo adakwera kuturuka mmadzi.....(Machitidwe 8V38,39). Tiwonsetse apa kuti mdindoyo adaona madzi ndipamene adafuna zoti abatizidwe. “Ndipo mdindoyo anati, Taonapo madzi ; chindiletsa ine ndi ndi chiyani kuti ndisabatizidwe?” (Machitidwe 8V36).

Chidali chodziwikiratu kuti munthuyu podziwa kuti ayenda ulendo wa mu mchipululu, padalibe chifukwa chokafunira madzi ambiri.

Ubatizo umatanthauza ‘kuchapa machimo (Machitidwe 22V16).Mfundo yoti munthu watembenuka zimafanana ndi kuchapa tikawerenga pa chivumbulutso 1V5;Tito 3V5; 2 Petro 2V22;Aheberi 10 V22.Chichewa choti kuchapa chikumveka bwino ngati tingati kumizidwa kusiyana ndi kudontheza.

Tinkamvetsetsa bwino ku chipangano chakale timamva kuti munthu ankavomerezedwa kwa mulungu ngati angasambe thupi lonse.

Ansembe ankasamba thupi lonse mu “mkhate” asadafike kufupi ndi mulungu (Levitiko 8V6; Ekesodo 40V32). A Israel ankayenera kusamba pa kudetsedwa ndi zinthu zina(Detoronome 23V11), zomwe zinkafanana ndi chimo.

Munthu wina ochedwa Naaman adali wa mitundu koma wakhate amene adafunaKuti achiritsidwe ndi mulungu wa mulungu wa a Isarael.Pa chifukwa cha ichiAkuyimira munthu wochimwa, amene ankayenera kufa ndithu.Kuchiritsidwa kwake kudali kukamizidwa mu mtsinje wa Yorodano.Poyambira chidali chovuta kwa iye kuti avomereze.poganizira kuti mulungu ankafuna achite chinthu china chapadera ,kapenanso kuti adziviike iye mu mtsinje waukulu ndi otchuka, monga ngati Abana) tikhoza kupulumutsidwa, kuposa kuti tibatizidwe mu mchiyembekezo choonadi cha Israel.Atamizidwa mu Yordan Naaman,thupi lake “lidabwereranso ngati limwana ndipo adachita“(2mafumu v9-14).

Apa tikhoza kumvetsetsa tsopano kuti 'ubatizo' umatanthauza kumizidwa titamvetsetsa Uthenga wabwino, monga momwe Baibulo lifotokozerwa, ubatizo sikuti umachita kufuna munthu wina wake waudindo wake mu mpingo kuti ubatize mzake. Ubatizo pakuti ndi pamene munthu amizidwa mmadzi atakhulupirira uthenga wabwino, nchotheke kuti adzabatize yekha. Komabe pakuti ubatizo ndi pamene munthu amvetsetsa chiphunzitso

Choonadi panthawi imene amizidwa, mpofunikabe kuti munthu wina omvetsetsanso chiphunzitsochi abatize mzake, iyeyutu ndi amene angamuyese mzakeyo ngati wadziwadi choonadi asadamuviike mmadzi. Ma Kristadefiya amayesetsa kukambirana ndi munthu amene afuna kuti abatizidwe makamaka asadamizidwe. Pamakhala mafunso angapo monga ngati amene tikuwawona kumapeto kwa phunziro lililonse. Nthawi zina amatha

Kuyenda mitunda yayitali chifukwa cha munthu mmodzi amene wabwera ku chiyembekezo chenicheni cha moyo wosatha, chifukwa sikuti cholinga chathu ndi kuchulukwa kwa anthu otembenuka ayi. Koma timafuna kuti ochepawo amene atembenuka akhaleli oti adziwadi choonadi.

10.2 KODI TINGABATIZIDWE BWANJI

Palitu maganizo osokeretsedwa pa nkhani ya ubatizo kuti tidzibatizana motani, makamaka wana, kapenanso kudontheza kapena kuwaza madzi pamphumi (Christening). Ichitu chimakhala chiyambi chosemphana ndi malembo a mu Baibulo.

Mau oti 'baptizo' ali mu chi giriki, amene amatanthauzidwa kuti 'baptize' (kubatiza) monga mmene Baibulo lidalembedwera. Mauwa sikuti amatanthauza kuwaza aii koma amatanthauza koma amatanthauza kuchapiratu ndi kumiza thupi lonse mu madzi kapena chirichonse chooneka ngati madzi. Mauwa ankagwiritsa ntchito pa sitima za m'madzi pamene zinkamira pamadzi 'baptized' (kumizidwa). Komanso amatanthauza pamene nsalu isinthidwa mtundu pobatizidwa kapena kumizidwa mu mankhwala (dye) kutitu nsaluyi isinthemtundu kudayenera kuti imizidwe yonse pansu pa mankhwalawo (dye)

osatitu dye (dye) mankhwalawo kuwazidwa pa nsalwai. Yohane 13 v 26 amatithandiza kuzindikira bwino mmene Ambuye adanyikira mkate mu vinyo. Kumizidwa ndiyetu zenizeni zotanthauza ubatizo monga mmene mavesi ammunsiwa akutithandizira kumvetsetsa zimenezi.

-Yohane ankabatiza ku Aenon kufupi ndi salim, chifukwa kudali madzi ambiri kumeneko: ndipo adaza, nabatizidwa (Yohane 3v 23) Izi zikutithandiza kuzindikira kuti pafunikira madzi ambiri kuti ubatizo uchitike; pakadakhlatu kuti padangofunika timadontho tamadzi, ndiye kuti pakadangofunika debe limodzi lamadzi pa anthu onse amene adafuna kubatizidwawo. Tikumvatu bwino pamene pa anthu adapita kumadziko mphepete mwa mtsinje wa Yordano kukabatizidwa, osatitu Yohane kupita kukawabatiza ali ndi botolo lamadzi mmanja ai.

-Yesu nayenso adakabatizidwa mu mtsinje wa Yordan- mu yordano (Marko 1 v 9) . Pamene Yesu adabatizidwa adatuluka (adavuuka) kuchoka m'madzi (Mateyu 3v13-16) Ubatizo wake apa ukuonekeratu kuti udali omizidwa -Ada-vuuka -- kuchoka m'madzi "Atabatizidwa ." China cha zifukwa zimene Yesu adabatizira kudali kutipatsa ife chitsanzo, kutitu aliyense amene afuna kutsata iye atengere chitsanzo cha ubatizo omizidwa.

-Komanso, Filipi ndi mdindo wa ku Efiyopiya "adalowa mmadzi---namubatiza. Ndipo pamene adavuuka kutuluka pamadzi----"(Machitidwe 8v38-39). Tikumbuke bwino apa kuti mdindoyo adafunsa za madzi pachithaphwi: " Taonani madzi awa: kodi chindiretsa ine kuti ndibatizidwe ndichiyani? (Machitidwe 8 v26) Ndiponso ndichodziwikiratu kuti munthu sangangoyenda mu chipululu osatenga madzi mu botolo . Pakadakhala kuti ubatizo ndi wowaza, sakanafunanso kupita ku chithaphwi aii.

-Ubatizo ndi kuikidwa mmanda (Akolose 2v12) Zimene zitanthauza kuundidwa. Ubatizo umatanthauza 'kuchapa' machimo (Machitidwe 22v16) Tanthauzo loti munthu watembenukadi zikufananitsidwa ndi kuchapa pa chivumbulutso 1v5; Tito 3v5; 2 Petro 2 v 22; Ahebri 10v22 ndi mavesi ena otere. Mau oti kuchapa akugwirizana kwa thunthu ndi ubatizo womiza kusiyana ndikuwaza.

Tikamawerenganso mavesi ena a muchipangano chakale amationetsa kuti mulungu amativomereza kwathunthu ngati tadzichapa (kusamba) Amsembe ankayenera kusamba thupi lonse pamalo otchedwa "Leva" asadabwere kufupi ndi mulungu pomutumukira (Levitiko 8 v6; Ekesodo 40v 32) A Israeli ankayenera kusamba kuti adziyeretse ngati adetsedwa.

Munthu wina wake otchedwa Naamani adali wa amitundu adali wakhate ndipo adafuna kuti achiritsidwe ndi mulungu wa Israeli. Iyeyu akuimira munthu ochimwa, amene ali oyembekezera kufa chifukwa cha uchimo. Ndipo kuti achiritsidwe adamizidwa mu mtsinje wa Yordano. Poyambirira adakhumudwa kwambiri kuti angathe kuvomereza namaganizira kuti mwina Mulungu akufuna kuti achite china chake chodabwitsa chamtundu wina kapena kuti akamizidwe mu mtsinje wina wake otchuka monga ngati Abana. Chimodzomodzinso tikhoza kuona kuti ndi chovuta kuti tivomereze kuti kungomizidwa pa madzi ndiye chingadzitse chipulumutso chathu. Komanso kuti tikhoza kuganiza kuti nechito zathu ndinso pokhala pamodzi kukumana ndi chigulu chachikulu chotchuka chalichi (Monganso ngati mtsinje wa Abana) tikhoza kupulumutsidwa , m'malo moti udzingokumana ndi kagulu koyembekezera chiyembekezo choonadi cha Israeli. Atamizidwa mu Yordano thupi la Naaman lidabwereranso mwakale ngati lamwana wang'ono, ndipo adayeretsedwa "(2 Mafumu 5v9-14)

Pongoona mmene malembo oonadi akutitumikiramu, sitingakaikensu kuti "ubatizoumatanthauza kumizidwa mmadzi monga mwa uthenga wabwino. Ngati mwamvetsetsadi, mutha kuona kuti sakutifotokoza za udindo wa munthu amene achiritsa kapena abatiza munthu obatizidwayo. Pakuti ubatizo umatifotokoza zakuti munthu amizidwe, nkotheke kuti munthuyo atha kudzibatiza yekha komatu mwa iyeyu munthuyo mutadzadza chikhulupiriro cha uthenga wabwino choonadi. Komabe popeza kuti ubatizo umayenera kuchitika ngati munthu uja wadziwadi choonadi, mpofunikira kuti pakhale munthu wina wapadera amene ali odziwa bwino choonadi kuti munthu ofuna kubatizidwa uja amuonedi ngati choonadicho wachidziwadi mokwana.

Pachifukwa cha ichi ma khirisitadefiya amapeza nthawi yokwanira yoti akambirane mozama ndi munthu ofuna kubatizidwa uja asadamizidwe pamadzi. Pamakhala ndondomeko ya mafunso ndi munthu ofuna lubatizidwa uja

asadamizidwe pamadzi. Pamakhala ndondomeko ya mafunso monga ngati amene tiwapeza kothera kwa phunziro liri lonse pamene pamagona maziko azokambiranazo. Amskhirisitadefiya amatha kuyenda mitunda zikwizikwi kukawona ndi kukambirana ndi munthu mmodzi amene amadziwa choonadi kuti munthuyo adzapeze moyo wosatha. Iwo cholinga chao sikuti amafuna kuti akhale ndi chigulu chotembenuka. Iwo amafuna osati kuchuluka ai.

10.3 TANTHAUZO LA UBATIZO

Chifukwa chimodzi pa zina chimene ubatizo uli kumiza pamadzi ndi chakuti umatanthauza kuyikidwa mmanda-monganso momwe Kristu adafera kutanthauza imfa yathu ku moyo wakale wa uchimo ndi kusazindikira kumene tidali nako. Povuuka mmadzi ku moyo wosatha pamene adzabwere, komanso pokhala moyo watsopano, mumzimu adagonjetsa chimo pamene Kristu adagonjetsa imfa ndi kuuka kwake.

"Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yache ?

Chifukwa tinaikidwa mmanda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa, mwa ulemerero wa atate, chotero ifenso tikayende mmoyo watsopano pakuti ngati ife tinakhala mchifanizidwe cha kuuka kwake"; (aroma 6 V3-5)

Tsopano pakuti chipulumutso chadza kudzera mu imfa ya Kristu yokha ndi kuuka kwake, ndi chofunikira kwambiri kuti tidziphatikize ku zinthuzi ngati tifuna chipulumutso, kufa ndi kuuka mwa Kristu, kumene timachita mophiphiritsa mu ubatizo, ndi njira yokhayo. Tizindikire kuti kudontheza madzi sizikwanitsa zinthuzi. Pobatizidwa, munthu wathu wakale (njira zathu zimene tinkayendera) zimakhomedwa pamodzi ndi Kristu pa mtanda (Aroma) 6V6) "Poukitsidwa limodzi ndi Kristu tidabatizidwa (Aefeso 2V5). Ngakhale ziri choncho, timakhalabe ndi umunthu tikabatizidwa, choncho ndi zomwe zimachitika nthawi ndi nthawi tikangobatizidwa, pachifukwa cha ichi Yesu adauza okhulupirira kuti atenge goli lake tsiku ndi tsiku ndi kumtsata iye, monga

mmene zidaliri, panthawi kukhomedwa pamtengo ndi Kristu siwapafupi ayi, ndi chokondweretsa kwambiri kuti ngati tingakhale mwa Kristu ndi zotheka kuti tidzauka naye.

Kristu adabweretsa " mtendere mu mwazi wake pamtengo paja "(Akolose 1V20" mtendere wa mulungu umene upereka kumvetsetsa "(Afilipi 4V7).Pa chifukwa cha ichi, Yesu adalonjeza kuti: " Mtendere ndikupatsani inu, mtendere wanga ndikulekerani inu: osati modzi adziko apereka mtendere (Yohan 14V27).Mtenderewu ndi chikondwerero cha uzimu chikuchotseratu zowawa ndi zovuta zimene tikufanitsidwa ndi kukhomedwa kwa pamtengo kwa Kristu: "Pakuti monga masautso a Kristu adatichulukira ife, choteronso chithokoza chathu chichuruka mwa Kristu(2 Akorinto 1V5)Palitu mtendere umene umadza chifukwa chakuti umunthu wathu wafadi, ndiyetu zikatero Kristu amakhala nafe wamee tiyetsedwa nthawi zonse.Paulo adalankhula atazionatu izi pamoyo wake: Ndinapachikidwa pamodzi ndi Kristu; koma ndiri ndi moyo; wosatinso ine ayi, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nawo tsopano mthupi, ndiri nawo mchikhulupiriro cha mwana wa mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha chifukwa cha ine"(Agalatiya 2V20)

Ubatizo utipulumutsa ife.... powukitsidwa mwa Yesu Kristu."1Petro 3V21) chifukwa tiri mwa Kristu, nafenso tidzaukitsidwa ku moyo wosatha pobwera iye.Apatu ndiye pagona chipulumutso chathu.Yesu adanena momveka bwino: Chifukwa ndiri wamoyo, inunso mudzakhala ndi moyo"(Yohan14V19).Paulonso ; " Tinayanjanitsidwa ndi mulungu mwa imfa ya mwana wache.....tidzapulumuka ndi moyo wake."(Kuuka;Aroma 5V10) .

Kawirikawiri zimanenedwa kuti poyanjanitsidwa ife ndi imfa ya Kristu ndi mazunzo ake mu ubatizo, ndi moyo wathu wa nthawi ndi nthawi, tidzagawana mu ulemerero wa nkuuka:- "Ngati tifa ndi (Kristu) tidzakhanso ndi moyo ndi iye; ngati tizunzika, tidzalamulira naye limodzi" (2 Timoteo 2 V11,12)

"Nthawi zonse tiri kusenza senza mthupi kufa kwake kwa yesu, kuti moyonso wa yesu uoneke mthupi mwathu.Pakuti ife amene tiri ndi moyo tiperekeka ku imfa nthawi zonse, chifukwa cha Yesu, kuti moyonso wa Yesu uoneke mthupi lathu lakufa.Podziwa kuti iye amene anaukitsa ambuye Yesu adaukitsa ifenso pamodzi ndi Yesu, nadzatiikapo pamodzi ndi inu."(2Akorinto 4V10,11,14).Paulo nayenso adazunzika ngati (Kristu) atakhala iye (ozunzika mmoyo wake) poyanjanitsidwa ndi zowawa zache, pofanizidwa ndi imfa yache; ngati nkotheka

ndikafikire kuuka kwa akufa monga mmene Kristu adachitira.(Afilipi 3 V10,11/Agalatiya 6V14)

10.4 UBATIZO NDI CHIPULUMUTSO

Ubatizo umatifananitsa ife ku imfa ya Khristu zikutanthauza kuti ndi mwaubatizo okhawo umene ungatithandize ife kuti tikhululukidwe . Tiri "Oikidwa mmanda pamodzi ndi (Kristu) mu ubatizo pamenenso mwaukitsidwa pamodzi ndi iye mchikhulupiriro cha machitidwe a mulungu, amene anamuukitsa iye kwa akufa.Anakupatsani moyo pamodzi ndi iye mmene adatikhululukira ife zolakwa zonse."(Akolose 2V12,13).Tinali osambitsidwa mu mdzina la Ambuye Yesu(1 Akorinto 6V11) -zikutanthauza kuti kubatizidwa mu mdzina la Yesu ndichokhacho chimene machimo athu amasambitsidwa.Izitu zikutibwezera kumbuyo pa Numeri 19V13, pamene anthu amene adalibe madzi odziyeretsera ankayenera kufa.Tidaonetsanso pa phunziro 10.2 mmene ubatizo uliri kuti umachapa machimo athu(onani machitidwe 22V16). Pamene tifotokozera za okhulupirira kuti amasambitsidwa ndi mwazi wa Khristu zikutanthauza kuchita ichi kudzera mu ubatizo (Chivumbulutso 1V5; kubadwa kwathu ndi madzi pa ubatizo(Yohane 3V5).

MPATUKO 30: KUBATIZIDWANSO

Anthu ena amaona ngati kuti ndichosayenera kuti ngati munthu udabatizidwa kale ndi ubatizo wina wake mongati kudonthezedwa madzi ali wamng'ono, kapenanso kumizidwa pamodzi ndi mpingo wina wake.Chotitu tidziwe apa ndi chakuti, munthu asdabadwe payenera kukhala kulapa ndi chikhulupiriro chenicheni cha uthenga wabwino(Machitidwe 2V38; Marko 16V15,16).Ubatizo umakhaladi ubatizo ngati zinthu izi zakhazikika mwa munthu asadamizidwe pamodzi.Mateyu 28V19,20 akutifananitsa ku ubatizo ndi zoti choyamba munthu ayenera kumva chiphunzitso cha Kristu chitafotokozedwa.Mwanatu wamng'ono sangathe kulapa kapena kumva uthenga wabwino; komanso kuwaza madzi siwubatizo ai.Mu chiphunzitso cha Baibulo, chifuniro cha munthu ofuna

kubatizidwayo ndiye zimamukhudza(mwachitsanzo abatizidwe chifukwa iwowo simwanayo ayi.Munthutu akhoza kudumpha ndi kugwera pamadzi ndi kumira kenaka kuvuka pamene akusambira apatu sikuti munthuyu wabatizidwa chifukwa sadamve ndi kukhulupirira uthenga wabwino.Chimodzimodzinso ngati munthu wamizidwa atakhulupirira zikhulupiriro zosiyanasiyana ndi Baibulo; ndiye kuti munthuyu wangomizidwa koma osati kubatizidwa.

Palitu chikhulupiriro chimodzi kutanthauza kuti uthenga wabwino oona umodzi, ndinso ubatizo umodzi- ubatizo umene umachitika munthu atakhulupirira" Chikhulupiriro chimodzi.Palinsu thupi limodzi (ndiye kuti mpingo oonadi umodzi)...monganso momwe mwaitanidwa mu chiyembekezo chimodzi, ubatizo umodzi, mulungu mmodzi(Aefeso 4V4-6).Palibe zoyembekezera ziwiri, monga ngati mmene anthu ena amene amati zomwe tikhulupirira ziribe nchito chifukwa mphatso yathu iri kumwamba kapena pansu pano.Palitu mulungu mmodzi-Yesu sikuti ndi mulungu ai.Zotsatira zake ndi zakuti, ngati tidabatizidwa titakhulupirira zosiyana ndi zimene Baibulo linena pachiphunzitso chofunika pa zinthu zofotokozera ufumu wa mulungu, mmene mulungu aliri ndi yesu Kristu ndi zina zotere ndiye kuti ubatizowo udalibe nchito.

Yohane mbatizi ankamiza anthu pamadzi , ndikuwauza kuti alape, ndikuwaphunzitsa zinthu zina zofotokozera Yesu Khristu (Marko 1V4),Luka 1V77.Komabe izitu sizidali zokwanira ai.Machitidwe 19V1-5 akuti ena amene adabatizidwa ndi Yohan adayenera kubatizidwanso chifukwa adali asadamvetsetse zinthu zina za chiphunzitso choonadi.Tikhoza kuzindikira kuti monga momwe ena amene adabatizidwa ndi Yohane, ifenso tazindikira kuti pamene tidabatizidwa koyamba sitidalape moyenera kuti tiyambe moyo watsopano.Ngati izi zitakhala choncho, sikuti ife tirephere kulandira choonadi tsopano ndi " ubatizo(oonadi) umodzi" umene ungachitike ngati talandira zonse zofotokozera chikhulupirir chimodzi choonadi.

MPATUKO 31: ZOYENERA KUTI TIDZIWE TISADABATIZIDWE

Anthu ambiri akhala akusokoletsedwa ndi magulu a Evangelical amene amanyozera za kufunika kwa zolembedwa mbuku lopatulika ku nkhani ya chipulumutso, namati munthu akangonena kuti ndikukhulupirira kuti Yesu Kristu ndiye mwana wa mulungu ndiye kuti iyeyo wapulumutsidwa. Mbuku la Machitidwe, zidalembedwa za mmene anthu ankatembenukira komanso maka maka za chikondi ndi kupirira zomwe ziri zofunikanso pa nthawi yathu ino. Tsopano timva za kufunika kwa chiphunzitso cha malembo.

MUKUTHAMANGIRA KUTI?

Tikawerenga buku la machitidwe limene tikumva za anthu ambiri amene adabatizidwa akuoneka kuti amaphunzitsidwa zinthu zofunika zochepe za ufumu wa mulungu, pongoti ndakhulupirira kuti Kristu ndiye mwana wa mulungu. Komatu tikaonetsetsa pa nkhani ya chipulumutso ngati titangonena mau atatu oti ndikhulupirira mwa Kristu sizikupereka tanthauzo lenileni loti munthu angapulumsidwe ndi ambiri a ma Evangelical amaganizo kuti payeneranso kukhala mzeru zina kapena chiyamiko mmaganizo a munthu amene akunena mauwa kuti akhale ndi tanthauzo. Mposavuta apa kuti timvetsetse. Komanso nkovuta, kuti, tisutse kuti mauwa amene avomereza kuti chikhulupiriro cha mwa Yesu Kristu ngati mwana wa mulungu ndiye chifunika. Aliyense amene amamvetsetsa mau a mulungu, angazindikirenso yekha kuti kungonena mau ochepe, posaganiziranso za zimene akumva ndi kukhulupirira, sizingampangitse kuti munthu akhale kuchipulumutso. Tiyeni tiwone mfundo zofotokoza za otembenuka mwamsanga zimene zingatithandize: Zolembedwa mbuku la machitidwe-komanso ndi mmalembo ambiri-zimamveka bwino kwambiri. Zimasangalatsa kwambiri ngati tikuwerenga mokweza zimene zinkalankhulidwa monga momwe mmachitidwe ndiye tawonani mmene nyengo yake iliri kuti tithe kuwerenga: apatu nchodziwikiratu kuti ayenera kuti amatenga nthawi yotalikira po powonjezerapo zimene sizidalembedwe : mwachitsanzo ;Mmene Paulo adadzitetedzera ku Yerusalemu zimatenga mphindi zinayi powerenga(Machitidwe 22); pamaso pa Fesito mphindi imodzi; pamaso pa Agripa pa mphindi zinayi; pamene Petro ankankhula pa Pentekosto padatha mphindi zinayi ; zoterozo kwa Koneliyo mphindi zitanu; Ambuye adalankhulanso atatha kudiyetsa anthu zikwi zisanu ndi zitanu. Mmene Petro adalalikira zenizeni zidali zoti nthawi imene adatenga polalikira ndi kutenga nkhanisi kuti ikafike kwa ansembe oyang'anira mu kachisi ndi kwa asaduki "

ndikuti nawonso afike ku malowa idali yaitali(Machitidwe 4V1) .Zimene Paulo adalalikira ku Aefeso zidalembedwa mwachidule ; kenaka , anthu a mmudzimu adandaula komatu mbali yauthengawu sudalembedwa mwa tsatanetsatane kufotokoza za kulalikira"Zinthu zoyenera za ufumu wa mulungu ndi kukwezedwa kwa Ambuye Yesu zidakhudza kuphunzitsa anthu kuti asiye izi.Enatu amati palibe chifukwa choyembekezera nthawi yaitali munthu asadabatizidwe ndicholinga choti aphunzire choonadi.Izitu sitingazipeze mmalembo ayi.Mphatso za mzimu woyera zothandiza kudziwa kuti athe kuzindikira maganizo a anthu, zinkathandiza olalikira anthawi imeneyo kuti athe kwawoko ndi kumene kunkawapangitsa kuzindikira bwino kuti munthuyu wadziwadi choonadi kapena ai ndipo akatero ankamubatiza. Pamene tikuwerenga kuti Ambuye Yesu mwiniwake ankaphunzitsa;tikutha kuwerenga kuti iye adayamba kuphunzitsa anthu ;izi zidachitika tsiku lonse koma pokumva zikukhala ngati nthawi yochepa-(Marko 6V34)

Palibe chifukwa choti tikhulupirire kuti maubatizo onse amene ankachitika ndi a Yuda ku Yerusalemu pa nthawi imene chi Kristu chinkayambika zida chitika mwapadera.Pamene Petro ankauza anthu kuti alape ndi kubatizidwa , khwimbi la anthulo, lidati, adali atamva kale kuphunzitsa uthenga umene adaumva kale poyamba.Palibe umboni oti miyanda miyanda ya maubatizowa ankachitika anthu asadaphunzitsidwe uthenga wabwino panthawi zakalezi.Chikadakhala kuti zinkachitika chonchi, ndiye kuti chi Kkristu chikadafalikira ku Yerusalemu kuja pa zaka zochepa kwambiri.Popeza anthuwa adali a Yuda akadakhala atadziwa bwino lomwe za chipangano chakale kumene kudawathandiza kudziwa bwino zonse.Tisadabwitsike pamene Paulo akunena za Melikisedi ngati ngati mau a Mkaka , pofotokoza kuti sakadatha kunena mwatsatanetsatane za iye chifukwa cha kusakhwima kwawo mu uzimu panthawi imene ankatembenuka , monga mmene Paulo akunena kuti sadali okhwima mmadziwidwe amalembo panthawi imeneyo.Zikuoneka ngati kuti makalatawa ankalembedwera makamaka ku ma Ekleziya a ku Yerusalemu ambiri a iwo akadayenera kubatizidwa mmasiku oyambira pamene ankalembe buku la machitidwe.

-Tikuyembekezera kuti tikuonetsa kuti kulalikira dzina la Kristu ndi kulapa monga mmene tikuwerengera ku machitidwe zikufanana ndi kumvetsetsa zonse za chiphunzitsa cha m'Baibulo.

1 Akorinto 15V24-28 akutiwonetsa za nkhani yokhudzana ndi zimene zidzachitike pomalizira pa milinyamu(zaka chikwi), komatu Paulo ponena akuonetsa ngati ndi zidziwika kale za chikhulupiro chimodzi zidalembedwa mu Baibul, ziyenera kuti mwina zidaphunzitsidwa kwambiri mu mpingo oyamba ndinso umboni wa uthenga wabwino kuposa zomwe adalemba.

DZINA LA YESU:

Dzina la mulungu likuphatikiza chiphunzitso chake ndi njira zake- maina a mulungu amaonetsa makhalidwe ndi cholinga.Chimodzichimodzi dzina la Yesu Kristu silingoseweretsa ayi koma LIRI NDI TANTHAUZO MU CHIPHUNZITSO chake.

Kukhulupirira dzina la Yesu zikufananidwa ndi kubatizidwa (Yohane 3V5,18,23).Agalatiya 3 V26,27 akutipatsa chikhulupiro cha mwa Kristu kugwirizana ndi kubatizidwa mwa iye: Inu muli ana a mulungu ndi chikhulupiro cha mwa Kristu Yesu.Pakuti ambiri ainu mudabatizidwa mwa Kristu mudavala Kristu.Zinanso zambiri zofotokozerana zitsanzo zogwirizana pakati pa chikhulupiro ndi ubatizo sikuti ndi nchito yokhayo yomumiza munthu mmadzi, komanso pafunika kudziwa zinthu zomwe ziphunzitsidwa mmalembo.

Filipiadalalikirira Kristu kwa iwo "(Machitidwe 8V5) zikumveka ngati akuti adangoti khulupirirani Yesu, koma Kristu akumasulidwa bwino pa machitidwe 8V12:"Pamene adakhulupirira Filipi akulalikirira zinthu za muufumau wa mulungu ndi dzina la Yesu Kristu, adabatizidwa, " Timvetsetse apa"zinthu" kunena zambiri osati chiganizo chimodzi chonena za Kristu; ndipo kulalikirira Kristu zikuphatikizanso chiphunzitso cha ubatizo .Pa Yohan 6V40 akutiwuzwa kuti ndichifuniro cha mulungu aliyense amene aona (amvetsetsa).Mwana , ndi kukhulupirira iye,akhoza kudza udza chifuniro cha (mulungu), adzadziwa za chiphunzitso cha mau"Yohane 17V17).Choncho kudziwa malembo ndichimodzimodzi ngati kuona mwana.Kristu akuti "Pakuti mwasunga mau anga, ndipo simudakane dzina langa"(Chivumbulutso 3V8) zikuonetsanso kuti mau a Kristu akufanana ndi dzina lake.

Kristu mouziridwa akutiwonetsera pounika Yesaya 42V4, ".....ndipo zisumbu zidzalindirira chilamulo chake"monganso "Akunja adzakhulupirira chilamulo

chake" (Mateyo 12V21), tsopanonso kuti dzina lake akulifananitsa ndi uthenga wabwino wa iye. Kalata wachiwiri ndi wa chitatu wa Yohane ali ndi zolembedwa zoti "Ngati uwape dzinali anaturuka osalandira kantu kwa amitundu (3Yohane 6,7). Apa tikubwereranso zimene adalembanso mtumwi Marko 16V15,16, kuti apite kukalalikira padziko lonse za uthenga wabwino; ndiye kutinso dzina la Kristu zikufanananitsidwanso. Kukhulupirira mwa Kristu' monga momwe malembo anenera zikuphatikizanso kubatizidwa. "Muli ana a mulungu mwa chikhulupiriro cha mwa Kristu Yesu. Pakuti (kutanthauza kuti chifukwa) monga ngati ambiri a inu mudabatizidwa mwa Kristu mudavala Kristu" (Agalatiya 3V26,27). Paulo akufotokoza ngati kuti pokhala iwo ndi chikhulupiriro mwa Yesu Kristu zikutanthauza kuonetsera chikhulupiriro chawo mu ubatizo. Ndiye kuti kukhulupirira Kristu ndi ndondomeko ya kumvetsetsa komwe kutsatizana ndi kumvera, osati kungonena pakamwa kuti 'ine sadzakhala ndi njala; ndipo amene akhulupirira ine sadzakhala ndi ludzu, "zimene zifanana ndi kuti kukhulupiriratu kuli ndi ndondomeko.

Chonchotu, kulalika Kristu kufunikira zinthu zosiyanasiyana za ziphunzitso. Ziphunzitso za Kristu ziripo (2 Akorinto 11V4; Agalatiya 1 V8; Yohane 7-12), komanso zinthu za mu ufumu wake (Marko 10V29 ndi Mateyo 16V28/Marko 9V1). Luka 9V11 akufotokoza za Kristu kulalikira za uthenga wabwino wa ufumu wa mulungu (Mateyo 4V23), pamenenso tikawona pa Marko 6V34 akutiwuzwa kuti iye adaphunzitsa zinthu zambiri chonchotu, uthenga wabwino umatanthauza zinthu zambiri chonchotu, uthenga wabwino umatanthauza zinthu zambiri osatu kungoti ndikukhulupirira Kristu pakanthawi kochepe. Timawerenganso kuti, "pamene adalalikira uthenga ku mudziwo, ndi kuphunzitsa ambiri (Machitidwe 14V21), kufananitsa kuphunzitsa ndi kulalikira. Kulankhula kotereku kudali kopanda nchito kukada kuti uthenga umene ukunenedwa apawu udali tiziganizo tochepe. Timamvanso tsiku ndi tsiku (ndi zolembedwa za chipangano chakale kapena?) kuti awonetsetse zimene Paulo adawaphunzitsa (machitidwe 17V11). Uthenga umene Paulo adaphunzitsa udagona pa chipangano chakale ndipo popeza kuti anthu aja adafufuzafufuza mmalembo a mbaibulo atatha kumvera iye, adakhulupirira -choncho ambiri a iwo adkhulupirira (Machitidwe 17V12). Pamene tikukambirana ndi anthu amene Baibulo saliwerenga tsiku lililonse, ndipo akudziwa pang'ono zimakhala zosakaikitsa poona kuti amasiyanso ndi anthu oyambirira aja." Amene

akhulupirira kuti Yesu ali "Mwachifuniro chake anatibala ife ndi mau amene ndi uthenga adalalikidwa kwa inu"(1Petro 1V23,25).Izi zikuonetsa kuti kukhulupirira kuti Kristu ali mwana wa mulungu chiri chinthu choti munthutu wamvetsetsadi uthenga umene uli mmau a mulungu.

MFUMU YA MAFUMU

Pakutsimikizira chikhulupiro cha mwa Kristu " kuti chikhale chatanthauzo mpofunika kuti tiyamikeso kuti udindo wa Kristu ukukhudzana kwambiri ndi ufumu wake.Ambuye yesu adawawuza Afalisi kuti padalibe chifukwa iwo adzikafunafuna kuti mpulumutsi ali kuti chifukwa adali atayimirira pakati pawo.Mauwa akutiufumu wa mulungu uli pakati panu"(Luka 17V21), kuwonetsa kuti ufumuwu ukugwirizana ndi mfumu ya mu ufumuwo.Pamene Yohne Yohane ankalalikira za kubwera zinthuzi ndi zogwirizana .Mau oti "ufumu wa kumwamba "pa Mateyu 3V2 komanso Luka 17V21 "ufumu wa mulungu (Daniel 2 V44); ndimwalawu/ufumu umene "udzasweke mutizidutswa ndi kuononga maufumu ena," kuwonetsa kuti mwalawo ndiye ufumu pamene uphwanye fano, komanso utaphwanya kale.

(d) Monganso mmene Daniel adaloserera, Ezekiel pa fanizo la mpesa akunena za mpesa wantete za mphukira zake zikuthothoka ndi kudzalidwa, kenaka ikudzakula kukhala mtengo waukulu, ndipo mmusi mwa mphukira zake mudzakhala mbalame ziri zonse za mapiko aliwonse,(Ezekiel 17V22,23).Izitu ziyenera kutanthauzira Kristu,"mtengo wathete pa Yesaya 53V2; zikugwirizananso ndi fanizo lake la mpiru, limene likufanizidwa ndi ufumu wa mulungu ku kambeu kamene kadkula ku mtengo waukulu umene mtundu uliwonse wa mbalame ungasale.Mgwirizano umenewu pakati pa mau a ufumu ndi Yesu mwiniwake ukuonetsa kuti iye mwiniwake adaona mau a moyo a ufumuwo.Pachifukwa cha chimenechi, ndizomveka bwino ndithu kuti "kukhulupirira mwa Kristu ndi kukhulupirira mu uthenga wabwino wa ufumu wa mulungu zikugwirizanadi.

KODI UTHENGA WABWINO NDI CHIYANI?

Tiyeni tidze ku zenizeni zimene okhulupirira oyamba akale adachiona ngati chofunikira kwambiri.Tidziwiretu kuti kudali chikhulupiro panthawi ya chipangano chatsopano chimene chikufanako ndi ndondomeko ya

chikhulupiriro" chathuchi.Chinanso chofunika kuchidziwa ndi kupezeka kwa abale amene adali ndi mphoto za uneneri-wonenera zakutsogolo zomwe zidali ndi chivumbulutso chochokera kwa mulungu pouziridwa.Mpoyenera kuti tikhulupirire kuti zina mwa zimene zidauziridwazi zidaikidwa ku chiphunzitsochi.

CHIPHUNZITSO

Paulo adati amene adali ku ekelezia yaa ku Roma"adakhulupirira kuchokera pansu pa mtima pao chimene chidaperekedwa kwa iwo"Aroma 6V 17)asadabatizidwe.Mau awa oti chimene akutanthauzanso kuti chomwe -monga ngati Paulotu poonetsa izi akutithandiza kuti timvetsetse kufunika koti munthu ayenera kudziwa bwino ndithu thupi la chiphunzitschoonadi asdabatizidwe osati kungoti Yesu ndiye mpulumutsi wanga ndikuthera pomwepo.Mu ekelezia yathu ena akhoza kukhala ndi makhalidwe a mulungu, koma akukana mphamvu yake "(2 Timoteo 3V5) komanso kuganizira kuti akhoza kusunga ziphunzitsozachikhulupiriro choonadi koma osazindikira mphamvu yeniyeni ya choonadi yimene ingawatsogolere, makhalidwe awo atsiku ndi tsiku .Paulo adakumbutsa a Galatiya kuti (Yesu Kristu waonetsedwa ndi kukhomedwa pa mtengo pakati pano"(Agalatiya 3V1).Mau oti waonetsedwa akutitsimikizira kuti wazindikiritsidwa mmalembo, kukhala ngati kuti zowalangiza za kwa Agalatiya zidali zodzera mmalembo.

Pofotokozerazachiphunzitsochakukuka kwakufu,Paulo akuti, Ndidapereka kwa inu.....zomwenso ndidalandira, za momwe Kristu adafa.....(1 Akorinto 15V3), izi ndi za momwe adalandilira chivumbulutso cha chiphunzitsochofunikira kwambiri kuti chikadakhala chabwino kwa iwo kusadziwa njira ya chilungamo kuposa.....kubwerera kuchokera ku lamulo lopatulika limene lidaperekedwa kwa iwo.Koma.....chidawayenera iwo cha nthawi yoono,Garu wabwerera ku masanzi ache, ndi nkhumba idasamba zimene zidaperekedwa kwa iwo zikugwirizana ndi kusamba kwa ubatizo ngati kuti njirayi ndi lamulo zidzadziwika asadabatizidwe.Taona kuti sikuti padali lamulo limodzi lokha loti munthu alimvetsetse pamene asdabatizidwe,chonchotu lamuloli limene likuoneka ngati limodzi likhoza kukhala ngati thunthu la ziphunzitsozolongosoledwa bwino zimene zidayenera kuzimvetsetsadi munthu asadabatizidwe.Palitu mavesi ambiri amene alankhula za kulandira zofotokozerazachiphunzitsochi.

za chiphunzitso cha uthenga wabwino." Agalatiya 1V9,12;Afilipi 4V9; Akolose 2V6;1Atesolanika 1V6;2V13;4V1.Izitu zikutsimikizira kuti uthenga wabwino udali ndi zinthu zenizeni zapadera zachiphunzitso zimenetu zidalandilidwa poyamba ndi atumwi kenaka ndi amene ankaphunzitsidwa.

CHIKHULUPIRIRO

Yuda adalankhula za chikhulupiriro chimene chidaperekedwa(kwa onse) kwa oyitanidwa (Yuda3).Chonchotu 'chikhulupiriro ndi chofanana ndi chiphunzitso ndi zinthu zoyendera limodzi zimene zidaperekedwa kwa iwo asdabatizidwe,, zinkachulidwa kuti thunthu la chiphunzitso .Paulo akutilalikira "kugwiritsa chikhulupiriro chathu(Aheberi 10V23) zimene zikutibweretsa kudzionetsera za chikhulupiriro tisadabatizidwe.Kusunga mau a chikhulupiriro (Tito 1V9) kuyenera kuti akunena za kugwiritsa za ndondomeko ya chikhulupiriro chimene adaphunzitsidwa.Chikhulupiriro chodziwikiratu"(Tito 1V4) chikutiwonetsa mmene thunthu la chiphunzitsochi chidafallikira kwa okhulupirira onse: chifukwatu padali chikhulupiriro chimodzi"(Aefeso 4V5).

Chikhulupiriro ndi dzina la Khristu zikufanana pa machitidwe 3V16.Taonatu kuti dzina la Kristu ndi dzina lomwe likupezeka mu chiphunzitso cha chikhulupiriro.Izitu zikutanthauza pa zochita zathu (1Timoteo 6V10) ndi chiphunzitso cha chikhulupiriro.Izitu zikutanthauza zochita zathu(1Timoteo 6V10) ndi chiphunzitso(1Timoteo 4V1).Paulo adachenjeza kuti ena adzapatuka pa chikhulupiriro, chifukwa cha chipatukochi ena akhoza kunena kuti chiphunzitsochi sitingathe kufotokoza kuti ndi chiyani.

ZOYENERA KUCHITA:

Zoyenera kuchita zidalinso mbali imodzi ya thunthu la chiphunzitso.Chikhulupiriro mwa Kristu zinkatanthauza kuganzira za chilungamo, makhalidwe ndi chiweruzo chiri nkudza(Machitidwe 24V24,25).Paulo akufotokozerza za kudya mgonero pamene ankaphunzitsa za kuuka kwa akufa:Ndidalandira kwa Ambuye zimene ndidapereka kwa inu.(Akorinto 11V23). Kwa akufa Pakuoneka kuti padalitu zinthu zoyenera kuchita, zimene Paulo kenaka adaonjeza chiphunzitso pakuoneka kuti padalitu zinthu zoyenera kuchita, zimene Paulo kenaka adaonjezera chiphunzitso cha malo wa a zichemwali mu ekileziya;" Sungani - zonse zimene ndidapereka kwa inu.Koma muyeneranso kudziwa kutimutu wa mkazi ndi

mwamuna....."(1Akorinto11V2,3.) .Izi zikuwonetsa kuti kufotokozerwa kwa zinthuzi kuyenera kuchitika munthu asadabatizidwe ndipo zidali mbali ya thunthu ya chiphunzitso chimene chidalimbikitsidwa mmasiku oyambirira akalero.Mu chigiriki mau oti zinthu zoyenera kuchita "zikutanthazidwa ngati malamulo a wanthu"pa 2 Atesalonika 3V6 ndi 2V15;"Mudzipatule... kwa m'bale amene sayenda..... monga mwalamulo adalandira kwa ife.....limbani mtima, gwiritsani lamulo limene mudaphunzitsidwa, kaya(ndi uneneri wowuzidwa) kapena kalata yathu.Izi zikuonetsa kufunika kwenikweni koti tigwiritse thunthu la chiphunzitso, ndinso kufunika kodzipatula kwa amene sakhulupirira izi:Kugwiritsa mau achikhulupiriro (uku ndikufotokozerwa kwa mtundu wina kunena za chiphunzitsochi) monga momwe adaphunzitsidwira, kuti athe kulalikira ndi kuwaopa onena nkambakamwa"Tito 1V9)

Tikudziwa padali aneneri onama "mmaekilezia oyambirira, amene ankanama zoti pali zivumbulutso kuchokera kwa mulungu za chiphunzitso chimene ankati ankayenera kuvomereza thunthu la chiphunzitsochi.Paulo akunenetsa mau a chikhulupiriro a chivumbulutso chouziridwa cha chiphunzitso(Tito 1V9;3V8;2Timoteo 2V11, 1Timoteo 4V9), chimene chiri choyenera kuvomerezedwa(1Timoteo 1V15;4V9)-izitu ziku tanthauza thunthu la chiphunzitso lokhala ndi chikhulupiriro ."Ndichifukwa chake Yohane adachenjeza kuti tisakhulupirire.... mzimu uliwonse umene adalitu ouzidwa (1 Yohane 4V1)

KUFOTOKOZERWA KWA PADERA

Tiyeni tiwone zitsanzo zina zachimvekere za ziphunzitso osati kungoti kukhulupirira mwa Kristu zidaphunzitsidwa kuti anthu azimvetsetse ngati tsinde la uthenga wabwino ubatizo usadachitike:

Mulungu adzaweruzwa zinsinsi za anthu ndi Yesu Kristu malingana ndi uthenga wabwino(umene Paulo adalalikira,Aroma 2V16).Chiphunzitso cha chiweruzo ndi udindo odzaweruzidwa ndi zinthu zenizeni zoyenera kuziganizira poyambirira-werengani machitidwe 24V25; Aheberi 6V1,2.

-Zoti mdulidwe udali ofunikira kuti munthu apulumutsidwe Paulo adatitu "udali uthenga wina"(Agalatiya 1V6) Pozindikiranso kuti sitiyenera kusunga lamulo la

Mose, monga ngati kusunga sabata, zidali zofunikira kuti munthu amvetsetse ngati uthenga wabwino oonadi.

-Uthenga wabwino wa ufumu " siuli wa Kristu yekha ayi komanso wa ufumu uli nkudza Yesaya 52V7(Aroma 10V15) zomwe zikufotokozera za olalikira uthenga wabwino onena za Zione, zoti "Mulungu wanu alamulira"-kutanthauza za ufumu.

-Ngati timvetsetsa bwino mfundo zina za memene Kristu adaliri ndi zinanso za chiyanjano (2Yohane 7-10).Timvetsetsanso apa kuti kungoti ndikuhulupirira mwa Kristu ziri zisakwanira

-Ndikofunikira kwambiri kudziwitsitsa za malonjezano udalalikidwa kwa Abrahamu(Agalatiya 3V8) ndinso kwa a Israel(Aheberi 4V2).Paulotu adanena polalikira kwake kuti malonjezano amene adapatsidwa kwa David adali mau a chiphunzitso"(Machitidwe 13V23,26).Zidalitu mabali ina ya uthenga wa chipulumutso "(Machitidwe 13V23,26).Zidalitu mbali ina ya uthenga wa chipulumutso.Iyetu akuti: Tikulamula(mau omwensu adamasulidwa pena ngati kulalikira kwa inu uthenga wabwino wa malonjezano omwe adachitika kwa makolo"Machitidwe 13V32). Komanso pa Aroma 1V1-4; .Uthenga wabwino wa mulungu..... za mwana wake Yesu, umene udali wa mbeu ya Davide.

-Kuti munthu amvetsetse malonjezanowa mpofunika kudziwa mbiri ya Israel; tikawerenga momvetsa bwino zimene Paulo adalalikira ku Antiokeya pa Machitidwe 13, timaonetsedwa kuti mbiri ya Israel; imanenetsa za malonjezano akwanitsidwa mwa Kristu Yesu.Kulalikira kwake kudagona ku mbiri ya Israel imanenetsa za malonjezano ndi zolakatula."ndipo potsiriza akutichenjeza ndi kutsatira zake pachiwerozo ngati tilephera kuvomereza kunena kuti ndizolakatula."ndipo potsiriza akutichenjeza ndi zotsatira zake pachiwerozo ngati tilephera kuvomereza kulalikira kwake (Machitidwe 13V40,41).Tiyenera kulalikira monga mmene iye adalalikira.

MAU OTSIRIZIRA

Kufunika kwa zonsezi ndi kwa mtengo wapatali"wonetsetsani kuti mukumvera chiphunzitso; muzichichita; chifukwa mukatero mudzadzzipulumutsa, ndi enanso amene akukumvani" (1 Timoteo 4V13-16).Zonse zimene zidaonetsedwa zofotokozera zomwe ziri mbali ya "chikhulupiriro" ndi zina zotero.Phunziro likutiwonetsa kuti palidi thunthu la chiphunzitso lomwe tonse tirivomereza mopanda chikaiko.Thunthu limeneli pophunzitsa limangolera munthu kuti

akhoza kubatiza ngati waonetsadi kuti wamvetsadi pokambirana momveka bwino.Nthawi zonse okhulupirira ankambikitsidwa pakati pathu.Ndipo tikalimbika pa chiphunzitsochi kapena kuwerenganso kawirikawiri, ndipamenetu tingapindule ndikulimbikitsidwa pakati pathu, monga momwe Paulo adanenera pa nthawi yake yamavuto adati.Ndatsiriza nchito yanga, ndasunga chikhulupiriroNdikumudzia amene ndidamukhulupirira, ndipo ndakopeka kuti atha kusunga zomwe ndamuchitira (pamoyo wathu) mpaka patsikulo (2 Timoteo 4V12)

NDEMANGA: KUVOMEREZA AMBUYE YESU:

Ngati muvomereza ndi pakamwa panu Ambye Yesu, ndi kukhulupirira mu mtima kuti mulungu adaukitsa iye kwa akufa, mudzapulumutsidwa"(Aroma 10V9)

Pali mfundo izi zimene tiyenera kuti zidziwidwe bwino.Tawonetsa kuti Ambye Yesu ngati achulidwa ndiye kuti akutiimira tsinde, kapena thunthu la chiphunzitsa cha zinthu zofotokozera ufumu wa mulungu ndi dzina la Yesu Kristu, kuphatikizanso ubatizo .Ayenera kuti adazindikira bwino momwe momwe akunenera pa Marko 16V16.Amene akhulupirira (Kuvomerezadi ngakhalenso ndi pakamwa/ ndi wabatizidwa(kuyuka ndi Kristu mwa akufa) adzapulumutsidwa.

-Kumvetsetsa za kuuka kwa akufa kwa Kristu zikugwirizana ndi kudziwa zomwe Baibulo likutiphunzitsa za Hade ndi ukhaliro wa munthu.

-Aroma 10V8,9 akuonetsa kuti pali kufanana ndi V13: "Pakuti amene adzaitana kwa (iye yekha) dzina la Ambye adzapulumutsidwa.' Paulo akunenedwa kuti adabatizidwa ndipo akuitana kwa iye yekha dzina la Ambye(Mateyu 28V19)

-Titatha ulimbikitsa zakufunika kwake kwa ubatizo monga ngati pa mutu wa Aroma 6, nkosathekanso kuti, Paulo yemweyo anene tsopano kuti kudali kosafunika kuti munthu abatizidwe kaya ndiye angadzapulumuke monga pa machitidwe 10.

-Aroma 10V9 akuyamba ndi mavesi awa 6-8; musanene muntima mwanu, adzakwera kumwamba ndani.....Adzatsikira pansu pa nthaka ndani....koma mau a chikhulupiriro, amene tiphunzitsa." Mau (a) chikhulupirirocho ndiwotu mau oyenera kuwvomereza, ndipo akufotokozera za ambuye Yesu pa V9.Taonanso kuti "chikhulupirirocho akutidziwitsa bwino bwino za thunthu la chiphunzitsa cha uthenga wabwino.Paulo adayamba waonanso pa Detoronomy 30 V11-

14.Lamulo ili ndikulumulani inu tsopano.....sikuti liri kumwamba...kapena pansi pa nyanja....koma mauwa ali pafupi ndi inu .Apatu akukhala, ngati akumasulira "mauwa"...kuti ali lamuloli kunenera za Kristu.Kusonyeza kuti a Israel akadasunga lamulori(mauwa) akadakhala odalitsika (Detoronome 30V16), chimodzimodzinsu a Israel atsopano akakhulupirira mau ofotokozera za Kristu adzatha kupulumutsidwa.Kuvomereza Kristu ndi pakamwa pathu zikugwirizana ndikulandira ndi mtima wonse chiphunzitso cha Khristu.Ngati mudzamvera mau a Ambuye Yesu ndi pakamwa panu.' Kufanafana kueneku kukuonetsa kuti ambuye Yesu ndi mutu otifotokozera za chiphunzitso chapa tsinde cha mau a mulungu.

MPATUKO 32:MBALA PAMTANDA PAJA

Mbala idati kwa Yesu adati kwa iwe, lero lino udzakhala ndi ine muparadizo.(Luka 23V42,43).Mavesiwa amatengedwa ngati akutanthauza kuti ubatizo siuli ofunika pa chipulumutso, ndinsu kuti timapita kumwamba tikafa.Poona ndi kuwerenga mozama tikuona kuti zinthu izi ndiye zoonadi:

- (1) Lamulo loti tidzibatizidwa mu imfa ndi kuuka kwa Kristu lidaperekedwa Yesu ataukitsidwa kale(Marko 16V15,16).Mbalayi idalibe pansu pa lamulo la Mose pamene Kristu adalankhula kwa iye.
- (2) Ubatizo weniweni oonadi ndi umene tiyenera kufa ndi kuuka ndi Yesu.Poonatu kuti pa nthawi imene Yesu ankalankhula kwa mbalayi izi zidali zisadachitike,ndipo kubatizidwa mwa Kristu kudali kovuta.
- (3) Ubatizo umafananitsidwa ndi kufa mwa Kristu (Aroma 6V3-5).Mabalayi idali yokhayo imene idachita izi.
- (4) Zikhozanso kutheka kuti mwina mbalayi , idali imodzi mwa anthu amene adabatizidwa pa ubatizo wa Yohane mbatizi:Ambiri amene adawatembenuza iye adali oti poyamba dzidali dzimbalangondo (Mateyu 21V32).Ngati ife tinena tsopano kuti mbalayi sidabatizidwe ndiye kuti tikutsutsana ndi zinthu zimene sizinatchulidwe, ndiye kuti tikutsutsana ndi zinthu zimene sizinatchulidwe penapaliponse.Koma nkosatheka kuti tipezereko mwayi kuti tisatsatire ndi

kumvera lamulo loti tibatizidwe.Chimodzimodzinso zamau oti"moyo kapena kumwamba sadalembedwepo pamene.

(5) Mbalayi idapempha Yesu kuti asadzamuiwale, pamene Yesu adzabwera kuzakhazikitsa ufumu.Mbalayi inkadziwa za uthenga wabwino wa ufumu wa mulungu umene Yesu adakhala akuphunzitsa (Mateyu 4V23).Ankadziwa kuti padzakhala tsiku la chiweruzo pozakhazikitsa ufumu, ndipamenetu adafunsa Yesu, pozindikiranso kuti iyeyo adzauka kwa akufa ndipo kuti iyeyo ndiye adzaweruze patsikulo, ndipo asadzamuiwale ayi, mbalayi idadzizwa zonsezi, iye adadziwitsitsadi; kuti opulumutsidwa patsiku loukitsidwa patsiku loukitsidwa ndi kuweruzidwa, adzaweruzidwa ndi mau ochokera mkamwa mwa kristu.

(6) Yesu adyankha kuti mbalayi idzakhala ndi iye mu "paradizo." Mau amenewa oti paradizo ndi a chigiriki ndipo amafotokozerana za zonse zimene zidzachitike padziko la pansi.Amanena za kudzakhazikitsanso munda wa Edeni umene udzaonekanso pamene ufumu wa mulungu adziza padziko la pansi(chivumbulutso 2V7).Panthawi ya ufumu wa mulungu, dzikoli lidzabweranso monga ngati mmene Munda wa Edeni udaliri ndinso ndi mmene zinthu zidaliri (Yesaya 51V3);Ezekiel 36V35) chifukwa panthawiyo temberero lidzatha(Chivumbulutso 22V3).Mau oti Paradizo amanthauza kukhala mwamtendere, mwachete, popanda chirichonse chovuta monga mmene kuchipangano chakale tikuwerenga pa Mlaliki 2V5; Nehemiah 2V8; Nyimbo 4V13;Genesis 13V10.Anthu ena azolembalemba ndi zolankhulalankhula adanenapo za paradizo yotaika ya Milton imenetu pokamba ankanena za kumwamba , komatu zidali zopeka chabe.Lonjezo la Yesu mbala kwa mbala ija la paradizo kudali kumuyankha zofuna zake zoti adzakhale nawo mu ufumu wa Kristuyo.Taphunziranso pa phunziro 5 kuti ufumu udzakhala padziko lapansi, choncho paradizo adzakhalsanso komweko.

(7) Pongoona ndi kumva za vesi 43,likukhala ngati kuti mbala ija ndi Kristu adzakhala limodzi ku paradizo patsikulo.Komatu ndi chodziwikiratu kuti ufumu sudzakhadzikitsidwe padziko lapansi.Sadaapita ku ufumu panthawi imene ija .Yesu adapita kumwamba(Machitidwe 2V32); monga momwe uneneri udanenedwera, adali panso pa nthaka "masiku atatu (Mateyu 12V40/16V21) itapita imfa ya pa mtanda.Ngakhalenso ataukitsidwa adati."Musandikhudze, pakuti sindidakwere kwa atate"(Yohane 20V17).Ndiyetu tikuona apa kuti Yesu sadapite kumwamba pamene adafa.

Yesu akuoneka kuti akulonjeza mbala ija "Lero lino udzakhala ndi ine mparadizo .Tiyenera uwerenga momvetsa bwino ndikuona kuti kodi mu chi Heberi ndi Chigiriki.Tikhoza kuwerenganso malo ena amene mauwa tingawamve mwamtundu wina" Yesu adati kwa iye, Indetu ndinena kwa iwe lero lino, udzakhala ndi ine mu Paradizo (Luka 23V43). Yesu adfunsidwa ndi mbala ija kuti adzaikumbukire kwa nthawi yonse patsiku la chiweruzo; adazindikira kuti yesuyo ndiye adzakhale mu ufumu .Ndipo adamutsimikizira kuti -ndikuuza tsopano: Sikutinso udikire tsiku lina za ine-udzakhala ndi ine mu ufumu!

(8) Kuchokera ku mfundo zimene tazionazi, kuli kofunikira kuonetsa chiphunzitso chimene mbalayi idamvetsetsa:

-Ufumu wa mulungu

-Kubweranso kachiwiri kwa Kristu

-Kuuka kwa akufa ndi chiweruzo

-Udindo

-Chipulumutso mwa chikhulupiriro mwa Kristu

-Ungwiro wa Kristu

-Kufunikira kotsata Kristu(adamutchula kuti "Ambuye")

Uchimo umene uli ndi munthu

Ndi chinthu chosayenera kuti tidzinamize kuti chitsanzo chathu ndi munthu ameneyu poganiza kuti munthu aliyense angapulumutsidwe atangoonetsa kamtima kochepe kofuna chi Kristu; Komatu payenera kukhala chiphunzitso chapadera chimene adali nacho. Popandatu ichi sadakakhala ndi chikhulupiriro chimene adali nachochi. Kristu sadapereke chipulumutso kwa mbalaija, imene idati "Ngati uli Kristu, dzipulumutse ndi ifenso."Koma padali munthu winayu amene adati "Ngati mwa Kristu muli phindu, sindikuona chifukwa choti ine ndirephele kupeza phinduli." Pachifukwa choti mbala ina ija idalibe chikhulupiriro sikadatha kupeza chipulumutso chenicheni kusiyana ndi ina ija.

MPATUKO 33: CHITSANZO CHA MWAMBO WA UBATIZO

Apa tingoonetsa maganizo ena amene ubatizo ungayendetsedwere bwino, onani ndondomeko ya ubatizo umene udachitika ndi ma Khristafediya ku Haartepoo, England pa tsiku loweruka mmwezi wa November 1990 cha ku masana. Ubatizowu udali omiza pa madzi kuwonetsa kulapa kwenikweni atakhulupirira uthenga wabwino. Mwambowu udali kungowonjezera kuti timvetsetse kufunika kwake. Zidayenda chonchi:

- Adayamba ndi pemphero
- Adawerenga Aroma 6
- Adafotokozeraza ubatizo
- pemphero
- Kumiza munthu mmadzi
- Pemphero

KUFOTOKOZERA ZA UBATIZO

Sitikukayika kuti tsiku la lero ndilofunika kwambiri mmoyo wa Dave; posachedwapa alowa pansu pa madzi pa madzi ndi kutulukansomwa Kristu, mbeu ya Abraham, ali ndi malonjezano a ulemelero amene akupangidwa ndi uthenga wabwino a kwa iye. Zikuoneka ngati zenizeni ayi pakuchita ichi, komatu Dave ndi ife tonse tiri pano tikuphunziradi kuti kumumiza mmadzi kumafaniziritsa iye imfa ndi kuuka kwa Yesu, monga momwe tawerengera pa Aroma 6V3-5" kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu tinabatizidwa mu imfa yache? Chifukwa chache tinaikidwa mmanda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa atate, chotero ifenso tikayende mmoyo watsopano. Pakuti ngati ife tinakhala olumikizidwa ndi iye mchifanizidwe cha imfa yache, koteronso tidzakhala olumikizidwa ndi iye mchifanizidwe cha imfa yache, koteronso tidzakhala mchifanizidwe cha kuuka kwache.

Kwa kanthawi kochepe tiyeni tiyese ndi kuganizira za mmene Yesu adaukira, chifukwatu pamene Dave adzavuuka kuchokera pamadzipa akhala atafanizidwa ndi kuuka kwa Yesu kuchokera ku imfa.

Tikhoza kuganizira mmene zidaliri mmanda muja ndi ulemelero umeneadali nawo mu moyo wake watsopano. Ayenera kuti adaona kuwala kwa ku Yerusalemu komatu anthu kumenekoko sankadziwa kuti kukuchitika chiyani kufupi ndi iwokuti munthu wina akuuka kwa akufa kwa akufa kumoyo watsopano.

Chimodzimidzinso pamene Dave akuvuuka pamadzi, anthu atizungulira sakudziwa kuti chinthu china chaulemelero chikuchitika ; kapena kuti akuona kuti kagulu kakang'ono ka amuna ndi akazi akupita ku dziwe ndikuti munthu wina akumizidwa pamadzi. Komatu monga momwe Angelo adasangalira pamene Yesu ankauka, chimodzimidzinso sitikuwaona, Angelo akukondwera kwa ochimwa mmodzi amene walapa.

Twerengatu pa Aroma 6 kuti tiyenera kuyenda mu moyo watsopano-chisangalalo chimene Dave akhale nacho tsopano chiptilire pamene ayenda mmoyo watsopanowu. Monga momwe tawerengera, sadzakhhalanso kaporo wa chimo, Dave tsopano wasintha bwana wake, ayamba kutumikira mulungu. Nthawi zina timaganiza kuti ngati takamizidwa ndi zochitika, sikuti tiri mfulu ayi, ndiye kuti tikutumikiranso chimo.

Paulo akufotokoza pa 1 Akorinto 10V1,2 kuti pamene tibatizidwa zimafanana ndi Israel pamene adadutsa pa nyanja yofiila. Anabatizidwa mu mtambo mu nyanjamo-mbali zonse ziwiri kudali khoma lamadzi. Pamene ankadutsa pakhozatu kukhala nthano pamenepa imene tingaphunzirepo. A Israel adakhala mu ukapolo ku Aiguputo, adkhala moyo wozunzika, nagwira nchito kwamphamvu muukaporowu ndikutumikira mafano a ku Aiguputo. Ndipo adalira kwa mulungu wawo kuti awapulumsa, ngakhale sankadziwa mmene akadawayankhira.

Powayankha mulungu adatumiza Mose kuti awatsogolere kutuluka ku Aiguputo, kudzera ku nyanja yoffira kenaka kudutsa mu chipululu, kuti akalowe ku dziko lapangano. A Israel ku Aiguputo kuja adali ngati Dave ndi ena onse amene amabatizidwa, tsopano Dave watsogozedwa kupita ku chigwa cha nyanja yofiira. Ndipo akudutsa mu madzimu, sikuti afikiratu ku dziko lapangano la ku ufumu ayi, tikhalanaye limodzi ifeyo kuyenda mu chipululu. Mulungu adatsogolera a Israel kuyenda mu mchipululu mwa Mngelo yemwe atizungulira, kutitsogolera ife mmiyoyo yathu ku chipulumutso (Masalmo 34; Aheberi 1V14)

A Israel adadyetsedwa manna tsiku lirilonse, amene Yesu akumasulira ngati iye mwini, ndi mau a mulungu pa Yohane 6. Akadakhala kuti sadadye ngati iye mwini, ndi mau a mulungu pa Yohane 6. Akadakhala kuti sadadye akadafatu mu mchipululu muja-palibe chakudya chirichonse. Mukufunsudwatu kuti nthawi zonse mudziwerenga ndi kuganizira zomwe mwawerengazo, maka maka, pakudya Kristu, amene mumpeza mmalembo onse. Mkofunika kuti tsiku ndi tsiku nthawi yofanana kuwerenga machaputala kenaka ndikuganizira mozama zimene zawerengedwazo kuti ngati tazimvetsetsa tizichite.

Pamene adali moyendamuna, a Israel adauzidwa kuti asasonkanitse manna wambiri patsiku limodzi, koma kuti aliyense kuti ndi tsiku adziyetsetsa kusonkhanitsa watsiku lokhalo. Chimodzimodzinso ifeyo tiyenera kuti tidzidya mawu a mulungu tsiku ndi tsiku. Monga momwe timadyera chakudya chathupi tsiku ndi tsiku osayiwala tidzidyanso/kuwerenga mau a mulungu tsiku liri lonse. Yobu adati, adawayetsa mau a mulungu oposa zonse ngakhalenso chakudya chake. A Israel adamwaso kuchokera ku mtsinje ochokera ku thanthe lija; Tikawerenga pa 1 Akorinto 10 timamva kuti thanthweli linkaimirira Kristu.

Nafenso tidzidya ndi kumwa muchitsanzo cha Yesu, zimene tingapange mwachikumbutso sabata ndi sabata ngakhalenso posonkhana, tiyeneranso kusonkhana ndi a nzathu amene tiri ofanana mchiyembekezo. Apaulendowtu ankati akamayenda mu chipululu amtha kukumana ndi kukambirana zofuna zimene akumana nazo ndinso zimene zikudza kutsogolo kwawo. Nafenso tiyeni tidzichita chimodzimodzi panthawi yino yamazunzo athu mu moyo uwu umene tiri pakatikati pa dziko lamavutoli posonkhana pamodzi. Ngakhale tiri patali wina ndi mzake tikhoza kulemberana makalata, kapenakuwerenga zolembedwa za anzathu.

Takamba za udindo wathu mu moyo watsopano, koma sikuti tidziganiza kuti tikangowerenga Baibulo, kamene kuchita zinthu zina ndiye kuti mulungu atipatsa mphotho ayi. Ndi cholinga cha mulungu mu chifuniro chake kutipatsa ife ufumu ngati mphoto yaulere, osati ngati malipiro a zimene tikuchitazo ayi (aroma 6V23). Sikuti tidziike kuti pakuti tabatizidwa ndiye kuti sitidzavutika kulowa mu ufumu. Ndi ulemelero wa mulungu tiyenera tidzikumbutse nthawi ndi nthawi kuti ndi choyenera kuti mukuwala kwa mulungu tiyenera kuti tidzimvera chikondi chake.

Pamene a Israel ankatuluka panyanja yamchere paja adasangalala kwambiri, Mose adayimba nyimbo ndipo anthu onse adakondwera. Masalmo 105V35-41

akutiwonetsa mmene mulungu adapereka zofunikira ku wanthuwa pa ulendo wawo:-

Ndipo zinadya zitsamba zonse za mdziko mwawo,(Iguputo) zinadyanso zipatso za mnthaka mwao.Ndipo iye anapha achisamba onse mdziko mwawo choyambira cha mphamvu yao yonse.Ndipo anawatulutsa pamodzi ndi siliva ndi golidi:Ndi mwa mafuko awo munalibe mmodzi wokhumudwa .Aiguputo anakondwera pakuchoka iwo ; ndi moto uunikire usiku.Anafunsa ndipo iye anadzetsa zinziri, nawakhutitsa mkate wakumwamba.Anatsegula pathanthwe, anatulukamo madzi.

Chikondwerero chimenecho ndi cha ife, abale ako amtsogolowa, tiri nawo pano kuchitira umboni , ubatizo wako.Ndi chikondwerero cha mulungu, cha Yesu ndi Angelo amene akutiwonerana pano tsopano.Tiyeni tonse tisunge chiyembekezochi ndi chikondwererochi"Mpaka potsiriza, kuti tikayende limodzi mu ufumu.

Tsopano tipita tikasinthe zovala zathu, kenaka ku madzi.....

PHUNZIRO 10: MAFUNSO

1. Kodi tingapulumutsidwe popanda ubatizo?
2. Kodi mau oti kubatiza amatanthauza chiyani?
 - (a) Kudzipereka
 - (b) Kuwaza
 - (c) Chikhulupiriro
 - (d) Kumiza
3. Kodi tanthauzo la ubatizo ndi lotani monga momwe adafotokozerera pa Aroma 6V3-5?
4. Kodi ndi nthawi iti imene tiyenera kubatizidwa?
 - (a) Titatha kuphunzira uthenga wabwino ndi kulapa
 - (b) Tiri mwana wamng'ono
 - (c) Titakondweretsedwa ndi Baibulo
 - (d) Pamene tifuna kulowa chalichi
5. Kodi timabatizidwa mu chiyani?
 - (a) Mutchalichi limene likubtizalo
 - (b) Mau a mulungu
 - (c) Kristu
 - (d) Mzimu oyera
6. Ndi zinthu ziti zimachitika ngati tatha kubatizidwa?
 - (a) Timakhala mbeu ya Abrahamu
 - (b) Sitidzachimwanso
 - (c) Timapulumutsidwa kwa nthawi zonse
 - (d) Machimo athu amakhululukidwa
7. kodi ubatizo okha ungapulumutse?

8. Kodi tidzalandira zozizwitsa za ulere za mzimu oyera titatha kubatizidwa?

PHUNZIRO 11

UMOYO MWA YESU

11.1 CHIYAMBI

Tikabatizidwa timakhala ndi chiyembekezo cheni cheni choti tidzakhala ndi moyo wosatha mu ufumu wa mulungu. Tikakhazikika mu chikhulupiriro chathu ndi chiyembekezo chapadera

Ndipamene timazindikira kuti pali maudindo ena pa ife. Zimenezi zimatifukulira ife kuti tiyeneradi kukhala ndi moyo oyenera kuti ifedi tili ndi chiyembekezo choti tidzadalitsidwa makhalidwe a umulungu (2 Petro 1 v 4) odzalandira dzina lake (Chivumbulutsa 3 v 12) podzasinthidwa kukhala angwiro mu zonse.

Monga tidzafotokoza mu phunziro 10.3 kuti titatha kubatizidwa tinadzipeleka pokhala amoyo wokhomera pamtanda zofuna zathu zoipa zamakhalidwe athu. (Aroma 6 v 6)

Ngati sitingayesetse kuchita izi ndiye kuti ubatizo wathu ulibe phindu. Mpofunika kuti munthu ngati afuna kubatizidwa akhale okonzekelatu kuti adzakhala ndi udindo wodzakhala mmoyo watsopano.

Pamene tibatizidwa timafuna mmoyo wakalewu umene tidabadwa nawo, ndipo mophiphiritsa timauka naye Khristu. "Ngati mwauka ndi Khristu (muubatizo) funafunani zinthu zammwamba, osati zinthu za pa dziko lapansi. Pakuti mwafachoncho lekani chigololo, zonyansa.....("akolose 3 v 5) Titatha kubatizidwa timayesetsa kudzipeleka ku moyo oona zinthu kuchokera kumwamba kwa mulungu, kuganizira za Mmwamba mwamba (ndiye kuti za uzimu), kuyesetsa kuleka kuchita za chilakolako cha thupi lathu zimene ziri zilakolako za mdziko pochita zofuna za mulungu ndi cholinga chodzalowa mu ufumu wa mulungu.

Cholinga chathu ndichoti tionetse mtima womvera Mulungu koma nthawi zambiri sizichitika. Nthawi zambiri mulungu amatichenjeza zoterezi. Pokamba za malamulo a mulungu, Iye amati "Zimene munthu achita, adzakhala ndi moyo ndi zomwezo " (Ezekiel 20 v 21) Ngati tizindikira malamulo a mulungu ndipo tiyamba kumvera mu ubatizo, tiyenera kuti tipirire powamvera mmoyo wathu wonse.

11.3. KUDZIYERETSA/ KUDZIPATULA

Oyera, Oyera, Oyera, ali ambuye (Yesaya 6v3.) Mau oti oyera abwerezedwa katatu pavesi limeneli zimene zikuonetsa kupatulika kwa mulungu. Kuyera kumatanthauza "kudzipatula" Kudzipatula kumeneku ndikudzipatula ku zinthu zodetsedwa ndikudziweretsa ku zinthu za uzimu. Tikulamulidwa kuti tikhale "otsatira zimene mulungu amachita " ngati tiwana take (Aefeso 5v1) Chonchotu "monga ngati amene akuyitana ali oyera inunso nkhalani oyera muzonse (kuthandauza muzochita zathu zonse mmoyo wathu); (1 petro 1v 15,16 ,Livitiko 11v44).

A isreali adaitanidwa kuchoka ku aiguputo kudzera ku Nyanja yofiira kukabatidzidwa kuti ankhale "dziko lopatulika"(ekesodo19v6) chimodzimodzinsu a Isreali mumzimu amalandira " kuyitanidwa koyera " ngati abatizidwa.(2 timoteo 1v 9).Titatha kubatizidwa " timakhala a kapolo odzipatula " (Aroma 6v19-22).

Monga ngati kudzipatula kuli kofunikira ngati anthu a mulungu, ndichinthu choyeneranso kuti onse amene " akusatira zochita za mulungu " atsatirensu. Ngati tingatero , "tizakhala ndi makhalidwe ake odziyeretsa" pamene tidzapasidwa makhalidwe ake (aheberi 12v 10; 2 petro 1v4).koterotu popanda kudzipatula mmoyo uno ,okhulupirira " sadzaona ambuye "(Aheberi 12 v 14) kutanthaudza kuti ngati munthu sadadzipatule mmoyo uno sadzatha kuona Mulunguyo mu ufumu wakewo.

Ngatitu tiri ndi chiyembekezochi tiyeneratu kukhala modzipatula ku zonyansa ziridzonse zotizungulira chifukwa amdzikowa alibe chiyembekezochi ,komaife tirinacho chimene chingatidzetsa ku umoyo wosatha odzalandira nawo makhalidwe a mulungu. 'kudzipatula' kwathuku kusakhale ngati tikuumiridzidwa; koma zikhale kuti Ifeyo tamvetsetsa chifukwa chimene

tikudzipatulira ku zamdziko zimene zatizungulira zimene zadzaza ndi zofuna zathupi .

Tiwone tsopano zinthu zina zimene tiyenera kudzimvetsetsa kuti tiyeneradi kudzipatula, kenaka mu phunziro 11.3 tiphudziranso zimene tapatuliradi .

KUGWIRITSA NTCHITO MPHAMVU

Tikukhala mu mdziko limene ladzazidwa ndi utchimo. Tidaphunzira pa chigawo 6.1 kuti maboma a anthu akhoza kutchedwa "mdierekezi chifukwa adakhazikitsidwa mu zofuna za thupi, amene m'baibulo timatcha kuti mdierekezi "

Baibulo limanena kawirikawiri, kuti, chimo ndi mbeu ya njoka zidziona kuti zikukula kula, pamene kunzuzika kwa panthawi yochepa munjira zosiyanasiyana, mbeu ya mkazi idzaoneka. Pachifukwa cha ichi okhulupirira aliyense akulamulidwa "kusakaniza kuti amzathu atichitire zoipa (Mateyu 5v39; Aroma 12v17; 1 Atesalonika 5v15; Petro 3v9)

Tinaonanso kuti zovuta zimene timakumana nazo zimachitika nazo zimzchitika chifukwa cha chifundo cha mulungu (Yesaya 45v7; Amosi 3v6 onaninsu Mphunziro 6.1)

Ngati ife tilimbana ndi kutsutsana zoti zovuta zikutichitikira:

Koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lako lamanja , umtembenzire linanso. Ndipo kwa iye wofuna kupita nawe kumlandu ndi kutenga malaya ako, umlolezenso chofunda chako."(Mateyu 5 v39,40) Khristu ndiye chitsanzo chathu: "Ndinapeleka msana wanga kwa omenya (Yesaya 50v6)

Khristu akukana kuti okhulupirira ake adzitengerana kumilandu chifukwa izitu ndi za mdziko. Posatengera mnzako kumilandu zimaonetsa kuti okhulupirira sabwezera zoipa ndipo ndi chitsanzo choti aliyense amene ali ndi chikhulupiriro chodzadza chamalonjezano cha mulungu choti ("kubwezera ndi kwanga ,"(Aroma 12v19) Usanene kuti ndibwezera zoipa, koma dikirani kwa mulungu, ndipo adzakupulumutsa iwe "(Miyambo 20v22/ Detorenome 32v35) Chidalitu chifukwa chimenechi chimene paulo adawatsutsa wa kiu akorinto amene ankatengera anzawo kumilandu (1 Akorinto 6v1-7)

Pozindikira kufunika kwa chiyembekezo chathu, tisakhudzidwe ndizopanda chilungamo zimene zikuchitika tsopano : Musatengerane kumilandu wina ndi mnzakesimudziwa kodi oyera adzalamula dziko? "(1 Akorinto 6 v1,2) Kutengera mnzathu kumilandu, kaya ndinkhani ya minda,kaya kuthetsa ukwati ndi zinthu zimene okhulupirira sayenera kuchita pamoyo wawo.

Anthu olamulira amaika anthu ngati apolisi ankhondo ndi ena kuti adzilepheretsa zovuta kuti zisachitike . Zoterezi ndi njira zina zimene okhulupirira eni eni sayenera kuchita. "Onse amene atenga chida adzafanso ndi chida (Mateyu 26vv52)

Ukulu ndi kungobwereza zomwe malembo akale anenera : Amene akhetsa mwazi wa munthu ndi munthunso mwazi wake udzakhetsedwa :.....Genesis 9v6. Ngati tikumuvutisa dala mnzathu ndiye kuti tikulimbana ndi mulungu pokha pokha ngati iye sadafune.

Mu umoyo wa chikhristu tikuuzidwa kuti kondani akukudani, dalitsani amene akutembererani chitirani zabwino amene akudani inu , pemphererani iwo amene akukuvutitsani inu (Mateyu 5v44; Luka 6v27) Asirikali ankhondo ndi apolisi amatsutsana ndi zimenezi chonchotu akhulupirira eni eni sangagwire ntchito ngati zimenezi. Ngakhalenso zochitika za m'mabungwe amenewa ngakhalenso nchito zimene zimafunika kuti tilumbire kwa akulu akulu, zimatsutsana ndi ufulu umene ulipo otumikira ndi kumvera malamulo a mulungu zisatikhuze ai. Okhulupirira oonadi amakanitsitsa kugwira nchito

NDALE

Pamene tili ndichikhulupiriro cha kubwera kwa ufumu wa mulungu chokhwima Ndikumvetsetsa kwenikweni zikutanthauza kuti tazindikira kuti maboma a anthu alephera kubweraetsa chilungamo pa dziko. Chifukwa cha ichi, sitienera kuti titenge mbali chifukwa tili ndi chiyembekezo cha ufumu uli nkudza . Yesu adaneneratu kuti zinthu zidzafika poipa "mmatsiku otsiriza " Panthawi yakuti iye ali pafupi kubwera (Luka 21v9-11, 25-27) Sizingatheke kuti munthu akhulupirire mau akeo komanso nthawi yomweyo akuyesa yesa kuti angakonze dzikoli. Fanizo la Msamaliya wabwino amatiphunzitsa mmene Mkhristu

angathandizire amdziko amene atizungulira- kuchitira zabwino kwa onse ndiye chofunika (Agalatiya 6v10)

Tikamawerenga za mnzathu okhulupirira oyambirira timamva mmene iwowo adakhalira mu moyo wa uzimu pamene akudikira kubweranso kwa khristu, makamakanso powatsimikizira kuti anthu amdziko powalalikira kuti nawonso adziwe sitiwerengatu zoti iwo ankatanganidwa ndi zothetsa umphawi, kapenanso kusintha makhalidwe akale ndikuti adzikhala makhalidwe amakono ai

Sizinthu mwa munthu kuti ayende munjira zake "(Yeremiya 10v23) chonchotu ndichinthu chamutengo wapatali kuti timvetsetse zoipa ndi zolakwa za umunthu siziyenera kuti iyeyo salitu oyenera ku munthu a lamulire . Pachifukwa ichi koponya voti chiri chosayenera pa anthu a mulungu. " Wankulukulu allamulira mmaufumu a anthu , ndipo aupeleka kwa iye Amfuna". (Danieli 4v32) Iyeyo ali wapamwamba kuposa anthu onse amene alamulira mmaiko (mlaliki 5v8).

Anthu amene ali pamipando masiku ano adaikika ndi mulungu (Aroma 13v 1) Ndiye ngati tiponya voti tikutsutsana ndi zimene mulungu adaika kuti agwire udindowu.

Tikumvanso bwino lomwe kuti mulungu adapeleka anthu ena mmanja mwa Nebuchadinezara kwa mfumu ya babulo. (Yeremiya 27v5,6)

Ndiyetu pakuti tikuzindikira kuti mulungu adapeleka mitundu ina kwa olamulira , tiyenera kuchenjera kuti tikhaledi mzika zenizeni, zokhala pansa pa malamulo adziko ku maiko amene tikhalawo , koma ngati zitsutsana ndi malamulo a khristu tisamvere.

Munthu aliyense amvere omulamulirachifukwa iwowa adaikidwa ndi mulungu, pachifukwa chaichi tiyenera kupeleka (Msonkho) komanso.....ulemu kwa amene ulemu ukuyenera "(Aroma 13v1-7) Ndipo ngati anthu ena amadzitcha kuti ndife akhristu namakatsutsana ndindale kapenanso kukana msonkho zikusonyeza kuti akulephera kumvera zophunzitsidwa zenizeni za m'baibulo. Penanso timamva kuti petro adamuletsa kuti asalalikire uthenga wabwino anthu olamulira pa nthawi imeneyo,iyetu adatsatira mau oti khristu akulamulira kuti ayenera kuchita: "chabwino ntchiti pamaso pamulungu kuti tiyenera kumvera mulungu koposa munthu... (Machitidwe 4v17-20; 5v28,29)

Mmenetu ma krista defiya adachitira pamene lamulo la anthu lidati apite kunkhondo chiyenera kukhala chitsanzo.

ZAM'DZIKO

Malingana ndi kutumikira mulungu ndi kukhala ndi chiyembekezo chenicheni chamtsogolo, dzikoli lapanga lili ndi zinthu zokoma zambiri za zomwe matupi anthu afuna .

Amene afuna kukondweretsa zofuna zawo ayenera kuzipatula kwa iwo akuyesesa kukula mum'zimu ,m'maganizo awo." Zofuna za iwo zofuna za thupi zitsutsana ndi mzimu, ndipo utsutsana ndi ndi zofuna zathupi (Agalatia 5 v 17) Pa chifukwa chakutsutsana kwa paderaku ndi chinthu chovuta kuti tizindikire zoti pamene tikuti tikutumikira zauzimu tikhozanso kumatayilira ndikutumikira za uzimu, tikhozanso kumatayilira ndikutumikira za thupi . Dzikolitu ladzazidwa ndi zambiri palitu" zilakolako za maso ndi zilako lako za maso, ndi zilakolako za moyo (1 Yohane 2v16)

(Amene akonda zamdziko ndi mdani wa mulungu) (Yakobo 4v4) Kukhala ndi abwenzi okonda zamdziko kuwonwra makanema a za mdziko ndi zina zotere , ndiyetu "Kuchita ubwenzi ndi zamdziko " zilako lako za mdziko ndi zakutha ndipo amene adzitsata pamoyo uno adzatha nazo (1 Yohane 2v15to 17)Anthu osachita za umulungu adzaonongedwa pobwera kachiwiri kwa yesu (2 Petro 2v5) Pakutitu " Dziko lonseli lidzadzidwa ndi zoipa " (1 Yohane 5v19) Ngati tikufuna kupewa kudzaonongedwa tiyenera kukhala anthu osakonda za mdziko (Yohane 17v16/Chivubulutso 18v4)

Zizolowezi zambiri zamdziko zotsatira zathupi zimachitika pongoononga umoyo wathu: kusuta fodya, kumwa mankhwala , osokoneza bongo ndi kumwa mowa mwa uchidakwa ndi zitsanzo zina . Umoyo wathu wathupi, Ndalama zathu zonse ndi zakwa Mulungu. Ndiye ndi chosayenera kuti tikhale ndi ufulu wodzigwiritsa nchito monga m'mene tifunira koma tiyenera kukahala audindo wa a zimenezi mulungu watipatsa .

Tidzafunsidwatu potsiriza pampando wachiweruzo (Luka 19v12-25) Zizolowezi zosuta fodya ndi kumwa mowa mwauchidakwa , ndikungoononga ndalama ndi moyo wathu. "Simudziwa kuti inu muli kachisi wa mulungu, ndikuti muzimu wa mulungu ukhala ngati wina adetsa kachisi wa mulungu, udzamuononga Mulunguthupi lanu liri kachisi wa mzimu woyera umene uli mwa inuinu simuli a unu nokhamudagulitsidwa ndi mtengo wapatali: choncho lemekezani

mulungu mu thupi lanu" (Akorinto 3 v16,17 ; 6v19,20) Ndiyetu kuononga thupi lathu chifukwa zizolowezi ngati kusuta fodya ndi zoopsya kwambiri.

Ndi zomvekatu kuti, zizolowezi ngati zikmenezi zidachitika munthu asadatembenuke, pakhoza kukhala povuta kuzisiya mwa nthawi imodzi. Chofunikira kwambiri ndi choti munthu mwa iye yekha azindikire bwino lomwe kuyipa kwa zizolowezi, ndipo kenaka azisiye osazichitanso. Zovuta zimene matupi athu angatikokeleko tiyenera kuzigonjetsa ndi mau a mulungu ndinso ndi pemphero, osatinso kedzera mwa munthu aliyense ngati ife.

11.3 NTCHITO YOYENERA KUCHITA MU CHIKHRISTU CHATHU

KUWERENGA MOZAMA BAIBULO

Titatha kubatizidwa tiyenera kuonetsa "zipatso mu mchiyero" kukhala mmoyo wotsogozedwa ndi mzimu wosati zofuna za thupi (Aroma 6 v 22; 8v1; Agalatiya 5 v16-25) Chimenetu chingatibweretsere ife ku chipatso chamzimu ndi kuzama nkuwerenga mau a mulungu ndipo mauwo akhalire mwa ife (Yohane 15 v7,8) Tikuonatu apa kuti timatsogozedwa ndi mzimu chifukwa chakuti muzimu wa mulungu uli mu mau ake. Ponseponse pamene tikukhala mmoyo wathu tiyenera kuti nthawi ndi nthawi tiri pafupi ndi mau a mulungu powerenga Baibulo mozama.

Ngati munthu awerenga baibulo mozama zimapangitsa kuti munthuyo azindikire bwino zakufunika kwa ubatizo ndipo amavomereza ndikuterodi : Tsopano tikangoterotu mauwo adzitiwongolera mu zochita zathu zonse mmoyo wathu ; Ubatizo ndi chinthu choyambirira mmoyowathu kuonetsadi kuti tamvera mau a mulungu . Ndi chinthu choopsa ngati ife tizindikira kufunika kwa kuwerenga

baibulo ndipo tikuterodi koma zotsatira zake za kudikira ziphunzitso zoonadi za uthenga wabwino zimakhala zotsutsana . Pachifukwa cha ichi tiyeneratu kupemphera mwachidule nthawi zonse tisadewerenge malembawa . "Ndisakuleni maso anga kuti ndizindikire zinthu zodabwitsa zam'malamulo anu" (Masalimo 119v18)

Mau a mulungu akhaletu chakudya chatu cha tsiku lililonse-Izitu ndizofunikira kuti kudalira kwathu m'mau a mulungu kukhale patsogolo kuposa chakudya chathupi lathu:

Ndakhazikika mmau ochokera mkamwa mwake kuposatu chakudya cha thupi langa "Yobu 23v12)"

Ngakhalenso Yeremiya adati " Mau anu ndidawapeza ndipo ndidawadya : ndipo mauwa adali kwa ine chimwemwe ndi chikondwerero mumtima mwanga" (Yeremiya 15v16) Tiyenera tikhale ndi nthawi tsiku lililonse loti tidziwerenga Baibulo ndichinthu ichi chikhale chizolowezi chofunikira ndi chapadera mmoyo wathu. Mphindi makumi atatu za mmawa ulionse zosasokonezwdwa zidzikhala chinthu choyambirira ndipo izi zitha kutiwongolera ku zochitika za uzimu ndipo zingatichititse ife kukhala anthu oyembekezera zenizeni pa tsiku la chiweruzo.

Pokana zoti tizingowerenga mbali imodzi ya malembo amene atikhudza kwambiri ma khristadefiya adapanga ndondomeko ya mmene tingathe kuwerengera baibulo;"mulozo wa Baibulo (Bible Companion) "(ikupezeka kwa amene adalemba bukuli). Mulozowu umaonetsa kuti tingawerenge mitu(machaputala) ingati patsiku; ngati titero ndiye kuti pakudzatha pa chaka timatha kuwerenga chipangano chakale kamodzi pachaka.Tikamawerenga choncho tsiku ndi tsiku , timakhala olimbikitsidwa kuti anzathu ena okhulupirira akuwerenganso chimodzimidzi.Pamene tidzakumana timakhala ndi mgwirizano weniweni; ndipo mitu imene takhala tikuwerengawo imakhala nkhani yotitsogolera kuti tiyenera tikumbutsane chiyani.Komatu tiyenera kuchenjera kuti pamene tiwerenga Baibulo tisangozitunga ngati zosewera.Koma kuti mauwa atilasedi mmoyo wathu.Yeremiya adati: " Mtima wanga wasweka chifukwa cha (Mau a aneneri: mafupa anga agwedezeke.....Ndiri munthu amene vinyo wadza, chifukwa cha ambuye, ndi chifukwanso cha mau a ulemerero wake" (Yeremiya 23V9). Adafanitsa mulungu ndi mau ake, chonchotu adamvatu kuti mulungu mwini adali pafupi naye pamene ankawerenga mau ake.

PEMPHERO

Chinanso choti tichimvetsetse choti tidzichita ndiye pemphero. Titazindikira kuti pali "mtetezi mmodzi pakuti pa mulungu ndi anthu, munthu Kristu Yesu; amene adapereka dipo ya ife tonse, ndipo Paulo akutsakula ife kuzindikira nchito ya Kristu: "Chonchotu ndipempha anthu apemphere pali ponse..... popanda mkwiyo ndi chikaiko "(1 Timote 2V-8)."Pakuti sitiri naye mkulu wansembe yemwe sangathe kumva chifundo ndi zofooka zathu; koma wayesedwa mzonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo. Poto tirimbike mtima poyandikira mpando wa chifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi nthawi yakusowa. (Aheberi 4 V15-16).

Zoonaditu ngati ife tikuonetsa kuyamikira kuti Kristu alidi mkulu wansembe wathu woti akupereka mapemphero athu mwa chisomo kwa mulungu, ziyenera kuti uzira ife kuti tidzimpempherera iye mchikhulupiriro. Komanso, sikuti mapemphero athu adzikhala opempha okha ayi komanso tizithokoza kwa mulungu tisadalandire chakudya, kuti tiyende bwino paulendo ndi zina zotero: ziyeneratu zikhale mbali ya makhalidwe athu kuti ndizipemphera.

Pamene tipereka zovuta zathu kwa Ambuye mmampemphero , pempheroro mukuthokoza onani kuti zofuna zanu zidziwike kwa mulungu. Ndi mtendere wa mulungu , umene uposa kumvetsa kwanu, udzapereka mitima yanu ndi maganizo anu (Afilipi 4V6,7).

Ngati mapemphero athu ali oti mulungu wafuna kuwalandira, adzayankhidwa (1 Yohane 5V14). Tikhoza kudziwa cha mulungu powerenga mozama mau a mulungu, amene amatiululira Mzimu wake/maganizo ake. Chonchotu ife mmene tingapempherere, zimene tingapemphere, zoterezi zimachititsa kuti mapemphero athu akhale amphamvu. Choncho mufuna, ndipo zidzachitika kwa inu " (Yohane 15V7). Pali zitsanzo zambiri za mapemphero mmalebo (Masalmo 119 V164; Daniel 6 V10). Kupemphera kwathu kwa mmawa ndi madzulo, ndi mau athu ochepa a zothokoza ngakhalenso masana zikhaletu zoti sitidathe kupemphera.

KULALIKIRA

Palitu chinthu china chapadera chimene chimadza pakati pa munthu amene wadziwadi mulungu oonadi, ndiyetu kukhala odzikonda mu mzimu. Tikhoza kukhutitsidwa kuti tiri pafupi ndi mulungu, chifukwa chowerenga Baibulo tokha ndi kukhala mu mzimu ndipo zikhoza kutichiritsa kuti tisagawireko anthu ena akhoza okhulupirira amzathu kapena otizungulira. Zimapezeka mmenemu, zimafanitsidwa ndi kuwala kapena nyali yowala mundima (Masalmo 119 V 105; Miyambo 4V18).

Kumeneku angabise, koma amaonetsa poyera (Mateyu 5V15).

"Inu muli kuwala kwa padziko" ngati tibatizidwa mwa "Mzinda umene wakhala pa phiri Suuli obisika," Kristu adapitiriza (Mateyu 5V14).

Ngatitu tukhaladi mogwirizana ndi uthenga oonadi taumvetsetsa, 'Kuyenera kwathu kumaonekera kwa otizungulira amene tikhala nawo. Sitidzakhumudwa kuti ifeyo "Tadzipatulira ku chiyembekezo cha ufumu, komanso tadzipatula kuchokera ku njira zamdziko zawo.

Mwa nzeru zathu tiyenera kuti tigawane zomwe tadziwa za choonadi ndi onse amene tikumana nawo; pamene tilankhula nkhani tidzitengera nkhani zathu ku zauzimu; kukambirana za ziphunzitso zoonadi ndi anthu ena a mipingo ina; kugawa mapepala a zolembe ziphunzitso zathu, ngakhale kukhoma timapepala tofotokozera za ziphunzitso zathu, zimene ziri njira zosiyana siyana zimene tingaonetse kuwala kwathu kuwanthu ena. Tisasiyire okhulupirira ena okha kuti adzichitira umboni mau oonadiwa ifenso ndi udindo wathu. Makhirisitadefiya ali ndi timagulu tochepa toonetsa kuwanthu ulaliki wathu kusiyana ndi magulu ena. Ndiye kuli koyenera kuti ifeyo, pa ife tokha, tiyetsetse pogwiritsa nchito zida zathu.

Njira ina imene ingatithandize kwambiri pakulalikira kwathu ndi pofotokozera anthu amene akazi kapena amuna awo sali mu chikhulupirochi ayenera kuti awafotokozere zikhulupiro zathuzi momveka bwino, ngakhale tikatero sikuti tingawaumirize kuti akhulupirire ayi. Mulungu safuna kuti titembenuze amzathu mochita kuumiriza. Udindo wathu ndi kuchitira umboni choonadi posayang'anira mmene anthu akuvomerezera. Tiri ndi udindo wapadera pochitira umboniwo (Ezekieli 3V17-21); chifukwa ngati Kristu angadze nthawi yathu ino "anthu awiri adzakhala mu munda; wina adzatengedwa" (Luka 17V36). Chikhoza

kukhala chodabwitsa ngati ife sitikuwafotokozera a m'banja athu ndi amene tikugwira nawo nchito za kubweranso kwachiwiri kwa ambuye.

MMENE TINGAKHALIRE MU EKELEZIYA (MPINGO)

Takhala tikuwerenga mozama mmene moyo wa mzimu uyenera kukhalira payekhapayekha. Ndi chofunikira kuti tidzisonkhana pamodzi ife amene tiri chiyembekezo chimodzi. Izitu ndizofunikira kuti nthawi zonse tidzichita. Tawonaso kuti titatha kubatizidwa timalowa mu mchikhulupiriro ulendo wopita ku ufumu. Nthawi zonse munthu akakhala pa ulendo, amayenda pamodzi ndi amzake a paulendowo, ndizimene timachita. Nthawi tiri ino yotsiriza pamene Kristu ali pafupi kudza; kudzathetsa zonse zimene ifeyo tikuona kuti sitingathe kuzithetsa; chifukwa cha ichi chiri choyenera kuti sitingathe kuzithetsa; chifukwa cha ichi chiri choyenera kuti tidzisonkhana ndi amene akudikiranso kuda kwake.

(10) Tisaleke kusionkhana pamodzi.....koma kulalikirana: pamene muona tsopano nthawi yayandikira "(Aheberi 10V25/Malachi 3V3V16). Abale ayeneratu kuyetsetsa kulemberana makalat, kuyenderana ndicholinga chokagawana mozama malembo a M'Baibulo, kunyema mgonero ndi zolalikira anthu ena.

Tonsefetu payekhapayekha "adaitanidwa kuchoka mu mdziko pokagwira chiyembekezo chapadera cha ku ufumu. Mau oti oitanidwa (saint) amatanthauzira anthu onse okhulupirira osati okhawa amene tikuwadziwa kale kuti adakhulupirira. Mau oti chalichi amene ali a chigiriki ndipo mu chingerezi admasulidwa ngati Ekileziya kutanthauza kusionkhana kwa oitanidwa kapena titi okhulupirira. Chonchotu mau oti chalichi amatunika kuti ndi gulu la okhulupirira, osati mmene ena amanenera kuti amatanthauza nyumba imene anthu amapempherera akakumana. Pokana kusokoneza ma Khristafediya amagwiritsa nchito mau oti ekeleziya osati chalichi.

Paliponse pamene pali kagulu ka okhulupirira, nkoyenera kuti apeze malo okumanirana nthawi zonse. Ikhozatu kukhala nyumba ya mmodzi okhulupirira kapena nyumba yobwereka padziko lonse lapansi, ma Khristafediya amakumana mu nyumba zochitira masewera, mu malo ochitira misonkhano, ku

hotela, nyumba zina zomanga okha, komanso nyumba zawo zogona. Cholinga cha Ekleziya ndi chokumanitsa pamodzi anthu ake kuti awerenge mozama Baibulo, komanso kudzionetsera ku a mdziko kuwala kwawo polalikira. Apa tiri chitsanzo cha mmene ma Khristafediya ayenera kuchitira.

TSIKU LOYAMBA

LASABATA(SUNDAY) -11 koloko mmawa-kudya mgonero.

-6 koloko madzulo -kulalikira anthu ena.

Tsiku lachitatu

-8 koloko mmawa -Kuwerenga Baibulo mozama

ali imodzi ya banja la mulungu .Pamene akukhala ndi chofunika kuti aliyense adzionetsetsa ndi kukhala odzichepetsa kwa mzake; Kristu adali chitsanzo chathu. Ngakhale adali otsogola pa zauzimu, ankadzionetsetsa kuti anali "kapolo wa onse." Adasambitsa mapazi ophunzira ake pamene iwo ankalimbana kuti wamkulu ndani. Yesu akutipatsa chitsanzo cha izi (Yohane 13V14,15; Mateyu 20V25-28).

Pachifukwa chakuti mphamvu za mzimu woyera zidatha, palibe chifukwa chokhala ndi akulu a mpingo (elders) monga ngati mmene zidaliri mmpingo yoyamba, "pakuti mmodzi ndiye wamkulu, Kristu; ndi inu nonse muli abale" (Mateyu 23V8). Pachifukwa mfundo imeneyi, Makhritafediya amadziwana ngati " mbale wa wina ndi mzake posayang'anira za maudindo ayi chifukwa pa za uzimu sikoyenera munthu kudzipatsa kapena kumpatsa wina udingo. Ifetu ndiye anthu ochimwa. Pamangokhala kuti timvetsetsetse ndi amene akhala atadziwa ndi kukhulupirira choonadi cha mulungu kwa nthawi yayitali kapena ngati zambiri za uzimu chifukwa cha kudzipereka kwawo mu za mau a mulungu komatu moyenera.

Zimene tiphunzira mu ekileziya yathu iyenera kugonera pa mau a mulungu. Amene alalikira mu ekeleziya amaonetsa makhalidwe a mulungu, ndipo alankhala mmalo mwa iye. Pachifukwa chakuti mulungu ali wa mwamuna, tiyenera kuonetsetsa kuti amene atsogolera amzawo mu ekileziya ali amuna chifukwa ndi zomwe akulankhula mau a mulungu. 1 Akorinto 14V34 akuti ululira zonse: "Akazi akhale chete mu mpingo :chifukwa sikuloledwa iwo kulankhula." 1 Timote 2 V11-15 amatifotokozeranso chifukwa chimene izi ziyenera kukhalira

choncho monga mmene ku munda wa Edeni zidaliri; chifukwa Hava adaphunzitsa Adamu kuti achimwe ; mkazi siayenera kuti aphunzitse mwamuna chimenetu mulungu adachita polenga Adamu koyamba asadalenge Hava ndichizindikiro choti "mutu wa mkazi ndi mwamuna(1 Akorinto 11 V3) , Choncho mu za uzimu mwamuna nkoyenera kutsogolera mkazi osatitu mkazi kutsogolera mwamuna.

Pachifukwa cha izi :Mkazi akhale chete modzichepetsa.Koma sindifuna kuti mkazi aphunzitse , kapena kulamulira mwamuna, koma akhale chete.Chifukwa Adamu adalengedwa koyamba kenaka Hava.Pakutitu Adamu sadanamizidwe, koma mkazi pakuputsitsidwa adachimwa.Komabe adzapulumutsidwa chifukwa cha kubereka, ngati apitirira mu mchikhulupiriro ndi mchikondi ndi mu mchiyero....."(1Timote 2V11-15)

Apatu tikuona kuti Baibulo likutidziwitsa zinthu zina zimene amuna ndi akazi okhulupirira ayenera kuchita.Azimayi pena akulamulidwa ku "kwatiwa, kubereka wana, kuyanga'nira nyumba (1 Timote 5V14) zimene zikuonetsa kuti mu uzimu wake ayenera kuyang'anira zapanymba .Choncho nchito yotsogolera ekeleziya ndi ya mwamuna.Zonsezitu ziri zosiyana kwathunthu ndi zimene munthu amaganizira ndi kulankhula zoti amuna ndi kavalidwe ndi machitidwe onse.Kusamalira ana amene abelekedwa mu banja kumafunikanso kuti onse awiri athandizane.

Okhulupirira enieni ayenera kuleka maganizo oti akazi okha ndiye ali ndi udindo onse.

Mwamuna asamuunjikire mkazi wake zonse, koma amkonde ngati mmene Kristu adatikondera(Aefeso 5V25).

"Amuna nu, khalani nawo monga mudziwira (kutanthauza kuti muwayang'anire malingana ndi mmene mudziwira mau a mulungu), kupatsa mkazi ulemu, monga ngati chida chofooka, monga ngati odzalowera pamadzi mu chisomo cha moyo"(1 petro 3 V7)

Mu zauzimu, kubatizidwa mwa Kristu zimafananitsa mwamuna ndi mkazi (Agalatiya 3V27,28/ 1 Akorinto 11V11). Komanso, chiri chachidziwikire kuti izitu sizikupangitsa kuti tiganizire kuti maudindo afanana ayi pozindikira zoti

mwamuna ndiye mutu mkazi"(1 Akorinto 11V13) mu zochitachita zonse mu uzimu pabanja ngakhalenso mu ekileziya.

Pofuna kuonetsa kuti izi zikugwiradi nchito, mkazi okhulupirira ayenera kuvala kumutu nthawi zonse m'bale wamwamuna akuphunzitsa mau a mulungu. Zimene zikutanthauza kuti kuvala chipewa kapena mpango kumutu ziyenera kutero pa kusonkhana kuli konse kwa mu ekileziya(mpingo).

Kusiyana kwa mwamuna ndi mkazi kuyenera kutsimikizidwa ndi mmene amuna ndi akazi asamalira tsitsi lawo(1 Akorinto 11V14-15). Mkazi aliyense amene apemphera.....ndi mutu ndi mutu wake osavala anyoza mutu wake(mwamuna wake) V3:Zifanananso ndi kuti iye wameta tsitsi lake."Koma mkazi yense wakupemphera , kapena kunenera , wobvula mutu , anyoza mutu wake; pakuti kuli chimodzimodzi kumetedwa. Pakuti ngati mkazi safunda, asengedwenso ; koma ngati kusengedwa kapena kumetedwa kuchititsa manyazi, afunde koma mkazi chifukwa cha mwamuna; chifukwa cha ichi mkazi ayenera kukhala nawo ulamuliro pamutu pache chifukwa cha Angelo.(akorinto 11V5,6,10)

Ngati ali osafunda akhala ngati wameta,"Kuwonetsa kuti mutu osafunda sikuti uli mutu opanda tsitsi ayi. Chonchotu mutu "ofunda sikuti ndi umene uli ndi tsitsi ayi, koma umene munthu moganzira kufunika kwake kofunditsa mutu wake. Ngati mkazi sadaike chofunditsa mutu wake, kwa mulungu chiri cholakwika. Ndi cholakwikanso kuti mwamuna afunditse mutu wake(1Akorinto 11V7); izi sizikutanthauza kukhala ndi tsitsi ayi, koma kukhala ndi china chake chofunditsira mutu wake.

Tikabwerera mmene mu chipangano chatsopano anthu amkakhallira azimayi ankamameta ngati apezeka kuti amachita chigololo kapena ngati mamuna wake wamwalira, chifukwa ngati mkazi wake kuti mwamuna wake wafa kapena ngati mkazi wafa kapena ukwati watha ndiye kufanitsa ndi kristu.

Mkazi ayimilira akeleziya, ndipo mwamuna ayimilira Kristu. Monga mmene tiganizira kuti machimo wathu abisika mwa Kristu, mkazinso ayenera kukhala oganzira kofunditsa mutu wake. Ngati mkazi akhulupirira kuti kofunditsa mutu wake kuli kofanananso kuti takhulupirira zachilungamo zathu kuti zizatipulumutsa monganso mwa Kristu. Poono kuti tsitsi lalitali la mkazi "uli (ulemelero wa kwa mulungu) kwa iye , chifukwa tsitsi lake lidapatsidwa kwa mkaziyo ngati chophimbira cha chilengedwe(1 Akorinto 11V15). Mkazi akulitse

tsitsi lake moonetsa kusiyana pakati pa iye ndi mwamuna pamene tiona kusiyana pa za kamangidwe ka tsitsi ndi zimene zikupereka kusiyana kwapadera.

Pa nkhani yimeneyi yoti mkazi adzisunga tsitsi lalitali ndi kufuna kumutu kwake, tikhaletu atcheru kuti tisangochita ngati chinthu cha dama ai. Ngati m'bale wa mkazi ali ndi uzimu oonadi ndikuti ali pansu pa kumvera (1Petro 3V5), ayenera kukhala pansu pa abale amuna monganso okhulupirira onse ali pansu pa abale amuna monganso okhulupirira onse ali pansu pa Kristu, ndiye kuti adziwonetsa mu zonse zochitika zake, kuphatikiza kufunda kumutu kwake. Ngatitu malamulowa amveka bwino bwino, monganso malamulo onse a Mulungu, sipangakhalenso cholephera kuwatsatira. Pali nchito zambiri mu ekileziya zimene abale a chikazi angagwire -kuphunzitsa Sunday sukulu, kapenanso kusunga za chuma ndi zina, zotero zimene sizikhudzana ndi kuyimilira pakati pa gulu losakanikirana pakati pa abale amuna. Muuzimu amai achikulire alimbikitsidwe kuyendetsa nchito yophunzitsa abale achikazi ang'ono (Tito 2V3,4/Onaninsu Miriamu adatsogolera azimai a ku Israel, Ekesodo 15V20).

KUDYA MGONERO

Pamene okhulupirira ali ndi chizolowezi chopemphera nthawi zonse ndi kuwerenga Baibulo, pafunikanso kumvera lamulo la Kristu lodya mgonero ndi kumwa vinyo pokumbukira msembe yake, chimene chiri chofunika kwambiri. Chitani ichi pokumbukira ine: Yesu adalamula (Luka 22V19). Cholinga chake chidali choti omutsatira ake adzachita kawirikawiri mpaka iye adzabwere. Kachiwiri, pamene Yesu adzagawane nawo (1 Akorinto 11V26 Luka 22V16-18). Ambuye Yesu adampatsa Paulo chivumbulutso chapadera zokhudzana ndi kudy a mgonero monganso za kuuka kwake (1 Akorinto 11V23/15V3); Chonchotu kudy a mgonero ndi kumwa vinyo ndi kofunikira kwambiri.

Chingwa chimaimirira thupi la Kristu limene lidaperekedwa pa mtengo paja, ndipo vinyo ayimimirira mwazi wake. (1 Akorinto 11V23-27). Izi zizisintha kwenikweni ku thupi ndi mwazi wake wa Yesu. Pamene Yesu adati "Iri ndi thupi langa" (Mateyu 26V26) timvetsetse kuti "zimaimirira, ichi ndi (chizindikiro) cha thupi langa." Mau oti "Ichi ndi" ndi akungonetseratu kuti 'Ichi chimaimirira' pa

Zakariya 5V3,8; Mateyu 13 V19-23,38; 1 Akorinto 11V25; 12V27; Luka 15V26; Machitidwe 2V12).Mau oti 'Ichi ndi' tiwamve ngati akuti 'Ichi chitanthauza kapena ichi chiimira." Okhulupirira oyambirira amadya mgonero kawirikawiri(Machitidwe 2V42,46), mwinanso kamodzi pa sabata (machitidwe 20v7) Ngati timukondadi khristu, tizimvera malamulo ake (Yohane 15v11-14) Ngati tili ndiubale weni weni ndi iye tidzafuna kukumbukira nsembe yake monga mmene adamfunsira, ndi kudzilambikitsa tokha pamene tikumbukira za chipulumutso chapadera chimene adakwanitsa. Pakanthawi kamene tikhala chete pakuganizira zowawa zimene adapeza pa mtengo paja zitipangitsa kuti mayesero athu akhalenso afanitsidwa ndi za mbuye wathu.

Pamene mgonero udyedwa chachikulu chimene chimachitika ndi kukumbukira basi, palibenso china chake chapadela chimene chimachitika. Zikufanana ndi paska panthawi ya lamulo la Mose (Luka 22v15; 1 Akorinto 5v7-8. Ichi chidali chikumbukiro cha kupulumutsidwa kumene adapulumutsidwa kuchoka ku Aigupto ndi kudutsa ndi mose pa nyanja yofiira. Ndipo pakudya mgonero zimatibwezeranso kumbuyo pamene tidapulumutsidwa ku machimo mwa khristu , zimene zidatheka pa mtengo paja ndipo timaphatikizidwa mu ubatizo . Tikasunga lamulori tizoloweratu nthawi zonse zoti ife tiyenera kuchita.

Pakudyatu mgonero ndi kumwa vinyo chimatipatsa ife chikondi cha khristu, komanso zinthu zonse zokhudzana ndi chipulumutso chathu, zimakhiladi zeni zeni. Pakudya mgonero kamodzi pa sabata ndi chizindikiro choti tiri a thanzi mu uzimu. Ngati tingalephere kukumana ndi okhulupirira anzathu mu choonadi, tichite tokha. Tisati tikulephera kukumbukira imfa ndi kuuka kwa khristu chifukwa anthu palibe ayi. Tidfziyetsetsa kuti tizikhala ndi chingwa ndi vinyo kuti tidzichita mwambowu nthawi ndi nthawi monga mmene kuyenera . Yesu adagwiritsa ntchito "chipatso cha mposa (Luka 22v18) ndiye tiyenera kugwiritsa ntchito vinyo wofiira.

Pakutenga zowawa za Khristu mu chingwa ndi vinyo imakhala msembe yolemekezeka ya wamkulukulu. Ngati tichita ichi pamene sitikumvetsetsa zimene zikuimira ndiye kuti tikulakwa, pakuti " ngati mudyu chingwa ichi, ndi kumwa chikho ichi muonetsa imfa ya Ambuyechoncho amene adzadya chingwa ichi, ndikumwa chikho ichi cha ambuye, mosayenera, adzalakwira thupi ndi mwazi wa a mbuye (1 Akorinto 11v26,27)

Nkoyeneratu kuti mwambo umenewu wa mgonero udzichitika pa malo amene ali osasokonezedwa ndi zopinga maganizo amunthu. Ikhozatu kukhala nthawi ya mmamawa, kapena usiku, kuchipinda ndinso malo ena oyenera. Tikulangizidwanso kuti aliyense adziyetse yekha, ndiyetu (modziyesa mofatsa) adye chingwa, ndi kumwa chikho (1 Akorinto 11v28) Tionetsetse kutimaganizo athu akhazikika pa msembe ya khristu, kapenanso poonetsetsa bwino malembo okhudzana ndi uthenga wabwino wa kukhomedwa pamtengo kwake, panthawi imene tili pafupi kudya mgonero. Tikachita ichi mwa ubwino ndiye kuti tiziyesadi ngati maganizo athu alidi pa khristu. Ndongomeko yoyenera kutsata pakudya mgonero ndiyotere:

1. Pemphero-Kupempha mulungu kuti adalitse kutsonkhana kwathu kuti atsakule maso athu ku mau Ake; kukumbuliranso zosowa zamzathu okhulupirira; kumuyamika iye chifukwa cha chikondi chake, makamaka chowonetsa mwa khristu, ndi kupemphera pa zinthu zina zimene tikuzisowa.
 2. Werengani baibulo pa ma chaputala atsikulo monga mmene aliri mu mulozo wathu.
 3. Ganizirani za maphunziro amene taphunzira kochokera kuzimene tawerengazo kapena werengani "Ulaliki -kuzama powerenga Baibulo za ma chaputala amene tawerengawo zimene tizibweretsa ku cholinga cha kukumana kwathu kukumbukira khristu.
 4. Werengani 1 Akorinto 11v23-29
 5. Kanyengo kochepa tikhale chete kodziyesa.
 6. Kuphemphera chingwa.
 7. Idyani chingwa ponyema kochepa.
 8. Pempherani vinyo
 9. Imwani pan'gono chabe
 10. Pempherani pemphero lotsiriza.
- Izi zikhoza kutha nthawi yongopitirira ola limodzi.

11.4 UKWATI

Tiyambe ndime iye poona amene abatizidwa ali okha asadakwatire kapena kukwatiwa. Tidaona kale pa Phunziro 5.3 kufunika koti okhulupirira ayenera kukwatira mzake obatzidwa ndi kukhulupirira choonadi. Pali zitsanzo zina za Yesu, Paulo ndi ena otero, kuti adawalimbikitsa amene adali osakwatira kapena kukwatiwa kukhala choncho malingana akudzipeleka nchito ya ambuye (1 akorinto 7 v7-9,32-38/2 Timote 2v4: Mateyu 19 v11;12,29; Mlaliki 9v9 ." Koma ngati mukwatira/mukwatiwa simudachimwe (1 Akorinto7v28) Apositole ambiri adali okwatiwa (1 Akorinto 9v5, ndipo monga ukwati ulili pa chifuniro cha mulungu umabweretsa chikhutiro cha zofuna za thupi ndi mzimu "Ukwati uli olemkezeka pazonse, ndipo sitidetsa pogona pathu("Aheberi 13v4) Ndi chosafunika kuti munthu akhale yekha koma ngati sangathe mulungu adakhazikitsa ukwati kuti athe kukwanitsa bwino za uzimu (Genesisi 2v18-24) choncho, "amene apeza mkazi apeza chinthu chabwino ndipo mulungu akondwera nawo--mkazi wa mzeru achokera kwa ambuye"Miyambo 18v22; 19v14)

Pali ndemanga yabwino apa "1 Akorinto 7v1,2: ndi choyenera kuti mwamuna asakhudze mkazi. Koma poopa kuchita chigoloro,mwamuna aliyense akhale ndi mkazi wake ndi wake, komanso mkazi aliyense akhale ndimwamuna wake ndi wake (v 9)

Tikamvetsetsa za mavesiwa akutifotokozera zoti ngati tikwanitsa zofuna zathu pogona ndi amuna kapena akazi ena tisadakwatire ndiye kuti tachita dama. Machenjezo otsutsana ndi dama (kugonana Kwa anthu asakwatira kapena osakwatira) , Chigololo pamene mwamuna kapena mkazi wokwatiwa agonana) Timaziwerenga kuti zinkachitika mu chipangano chatsopano pafupifupi buku lililonse limadzudzulapo za zimenezi . Zina mwa izo ndi izi, Machitidwe 15v20; Aroma 1 v29; 1 Akorinto 6v9-18; 10 v 8; 2 Akorinto 12 v 21; Agalatiya 5 v 19; Aefeso 5v3; Akolose 3v5; 1 Atesalonika 4v3; Yuda 7 ,1 Petro 4 v3; Chivumbulutso 2 v21.

Tikamamva zolembedwazi zikubwerezedwa bwerezedwa, kulikofunika kuti tikhale omvera mulungu. Zolakwa zimene zimadza chifukwa kufooka kwathu,

mwachisomo cha mulungu, ngati tilapadi ndi mtima wathu wonse mulungu amatha kutikhululukira (mwachitsanzo chigololo chimene Davide adachita ndi Betiseba) Koma ngati tikhala moyo wochita izi ngati chizolowezi, mulungu akwiya nafe ndipo adzatichotsa mu buku lamoyo. Paulo adati "Chigololo, dama, ...ndi zina zotero zimene ndikuuzani (Chiweruzo chisanadze), monganso momwe ndidakuuzirani poyamba, kuti amene achita izi (nthawi zonse) sadzalowa mu ufumu wamulungu (Agalatiya 5 v 19-21)Choncho, patukani ku dama (2 Timoteo 2 v 22) Chimo lililonse limene munthu achita achita popanda thupi , koma amene achita za dama achimwira thupi lake ")(Akorinto 6 v 18) Padziko lonse lapansi ena amatha kuvomereza kuti anthu azitha kugonana asadakwatilane . Izi ndi zosayenera kwa okhulupirira . Okhulupirira choonadi ayenera kuchita ukwati wake monga momwe mulungu adalangizira ; tisatsanze zofuna zathupi zimene anthu akunja atsatira zimene zitsutsana ndi zolemba za mulungu. Komansotu ukwati udakhazikitsidwa ndi mulungu osati munthu. Mu baibulo, ukwati uli ndi zinthu zitatu:.

1. Payenera kuchitika ndondomeko ya ukwati ingachepe ingatani . Tikawerenga za ukwati wa Boazi ndi Lute pa Lute 3v9-14 :13 zimene zikuonetsa kuti ukwati sichinthu choti tingotibasi ukwati wakhala koma payenera kukhala nthawi yabwino ndithu kuti munthu wakwatire kapena wakwatiwe . Khristu amafanitsidwa ndi mkwati ndi okhulupirira a kwatibwi , amene adzakwatire"pakudza kwake kachiwiri.Padzakhala madyerero a mwana wa nkhosa'pokondwerera (chivumbulutso 19V-9) Ubale pakati pa mamuna ndi mkazi zifanitsidwa ndi ubale pakati pa mwamuna ndi mkazi zifananitsidwa ndi ubale wapakati pa Kristu ndi okhulupirira (Aefeso 5V25-30). Monga padzakhala ukwati pakati pathu payeneranso kukhala ukwati pakati pa okhulupirira amene ayamba ukwatiwu, kufananitsa mgwirizano wa Kristu ndi ifeyo pa tsiku la chiweruzo.
2. Ukwati wa mulungu ndi Israel udali oti adpangana zoti adzmvera mwa chikhulupiriro (Ezekiel 16V8), izi ziyenera kuwonekeranso ku zaukwati wa okhulupirira.
3. Kugonana kuli kofunika kulimbikitsa ukwati (Duteronome) Genesis 24 v 67 ;29 v 21 ; 1 mafumu 11 v2) Pachifukwa cha ichi , 1 Akorinto 6 v15 ,16 akufotokoza chifyukwa chake kugonana kwa anthu amene sadakwatirane kuliri kolakwika . Kukhala pamodzi kwa mwamuna ndi mkazi kumasonyeza mmene mulungu wakwatitsira anthu

awiri (Genesis 2 v 24) Kukhalira pamodzi ngati" thupi limodzi " kwa kanthawi kochepa ndiye kuti sitigwiritsa ntchito bwino matupi amene mulungu watipatsa . Matupiwa adawapanga kuti agwirizane zimene iye waphatikiza pamodzi pa ukwati.

Titatha kumva izi tikuona kuti anthu amene akhalira pamodzi asadakwatirane ndiye kuti akuchimwa. Pokha pokha atakonzanso bwino mgwirizano wawo kuti ukwati wawo ukhalenso bwino - atha kubatizidwa koma ngati satero sangathe kubatizidwa ayi.

Palitu kusamvetsetsana kumene anthu amene ali mmaiko amene akubwera kumene koti satha kuganizira zoti ukwati ulionse udzikhala ndi dongosolo lenileni loyenera . Amatha kukhala zaka zambirimbiri osachita dongosolori namati ali paukwati. Tikungolangiza pano kuti munthu amene tikufuna kumubatiza timufotokozere bwinobwino , ndi kuti alembe penapake kuvomereza kuti adakwatirana.

Ukwatiwu uyenera kuti akulu akulu amaudindo wawo asayinire kuti ndiukwatidi.

Amene adabatizidwa, mkazi kapena mwamuna wake asadatero, asamusiye kuti ukwati watha ayi. (1 akorinto 7 v13-15), koma tiyetsetse kuwakonda , ndikuwaonetsa kuti iwowo alidi ndi chikhulupiro choonadi, osati adangofuna kusintha mpingo ayi. (1 Petro 3 v1-6) akulimbikitsa kwa amene alimu zotere ndi mkazi kapena mwamuna wakunja kuti atha kuvomereza choonadi chimene mzake wabanjaya ngatidi akuonadi mphatso zake.

Zokhudzana ndi ukwati Mulungu akutidziwitsa kuti "Mwamuna adzaleka atate wake ndi amayi wake ndipo adzaphatikizana ndi mkazi wake; ndipo adzakhala thupi limodzi. (Genesis 2 v 24) Pamene tikukamba za mgwirizano pakati pa mwamuna ndi mkazi tiyeneranso kuyetsetsa kuti tikhalenso ogwirizana ndi khristu , pogonjetsa utchimo ndi kudzikonda kwa chilngedwe chathu. Chigonjetso chimenechitu ndi cha ife tokha eni ake osati khristu kapena mnzathu wam'banja ai. Ngatidi tingagonjetse zitipingazi, tidzakhala okondwa ndipo kukwanitsa ubale wathu ndi khristu.

Komabetu tiri pakati pa anthu akunja, amdziko kumene tchimo ndi zofooka zathu ndipo timalephera kukwanitsa zimene Baibulo likutiphunzitsa monga mwa chikondi chimene mulungu ndi khristu atisonyeza. Zomwe tikulangizidwa pa

Genesis 2 v24 ndi zakuti mwamuna m'modzi ndinso mkazi mmodzi kukhala pamodzi mogwirizana kwamoyo wawo wonse.

Okhulupirira ayenera kuzindikira kuti sangathedi kukwanitsa monga momwe zifunikira mu moyo wawo kapenanso kwa okhulupirira ena. Amuna ndi akazi atha kusemphana maganizo ndipo mgwirizano uja ndi kutha; Nthawi zinanso mwamuna akhoza kukhala ndi akazi ambiri kumadera amene amavomereza izi. Akaziwatu ayenera ayenera kukhala amene adakwatira asadakwatira asadabatizidwe. Ngati zinthu zingakhale chonchi, ayenera kukhala nawo, nawasamala ngati m'mene ngati m'mene angakondwere ndi mkazi mmodzi, koma asakwatirensa wena wowonjazera pamenepa. Mtumwi Paulo, amene adathanso kumvetsetsa zovuta za anthu adatsimikizira mfundo zauzimu zofunikira ndipo adalangiza anthu kuti kusiyana ukwati kukhoza kuchitika munthawi zina ngati zalepherekatu kupirira:

Mkazi asasiyane ukwati ndimwamuna wake koma ngati asiyana, akhale osakwatiwa "(1 Akorinto 7v10-11) Ngati tamvetsetsa malembo awa, tiyenera kuti tivomereze chifukwa zalembedwazi ndi za wankulukulu (mwachitsanzo zoti chigololo ndi cholakwa) Langizo limene Paulo adapeleka pa 1 Akorinto 7v10-11 ikugwirizananso ndi 1 Akorinto 7 v27, 28 Kodi sudamasulidwe kwa mkazi? Leka kufuna mkazi (kutanthauza kuti tisakwatire) koma ngati ukwatira /ukwatiwa sudalakwire " komabe kuthesa ukwati ndikulakwira zomwe mulungu afuna zoti adziwe munthu ndi zakuti chimene mulungu adamanga choti ndi thupi limodzi ndi chomwecho ngakhaletu ziri zovuta kuzichitadi.

Kuyambira pachiyambi Mulungu adawalenga iwo mwamuna ndi mkazi. Pa chifukwa chaichi adzasiya atate wake ndi amayi wake, ndikuphatikizana ndi mkazi wake ndipo awiriwa adzakhala thupi limodzi: ndiyetu (Yesu akutsimikiziranso) salonso awiri ayi koma thupi limodzi. Chonchotu chimene mulungu wamanga palibe munthu angamasule (kuthetsa ukwati).....amene adzaleka mkazi wake nakwatira wina achita chigololo kwa iye. Ndipo ngati mkazi asiya mwamuna wake nakakwatiwanso ndi wina, achita chigololo (Marko10 v6-12)

Pankhani ya zaukwatiyi, thupi limadziimiriza kutsatira zofuna zakezo, monga mwa chilengedwe. Ndiyetu amene ayesedwa mu ziznthu ngati izi choyenera kuchita ndikungobwerera kumalembowa kawiri kawiri monga tawonera

pamwambapa. Ena amachita njira zosiyanasiyana pofuna kukwaniritsa zofuna za thupi lawo, monga kugonana amuna okha okha ndi zina zotere. Izi ndi zosavomereka ndi mulungu.

Chifuniro cha mulungu kawirikawiri munthu safuna kuti achitstire ndipo amayetsetsa kuchita zomwe iye munthuyo afuna, namafananitsa ndi zamulunguzo. Zonsezi ndi zomulakwira mulungu. Tikawerenga pa Genesis 2v24 tikuona tchimo logonana amuna okha okhai ndi cholinga cha mulungu kuti mwamuna ndi mkazi akwatirane ndi kuphatikizana. Mulungu adalenga mkazi kukhala othandiza Adamu, osatinso mwamuna nzake ai. Zogonana amuna okha okha zili zokanidwa kotheratu ndipo baibulo likunena tchimo limeneli lidali limodzi la machimo amene mulungu adaonongera Sodomu (Genesis 18-19); Ndinso mtumwi Paulo akuti ngati tichita zizolowezi zimenezi, ndiye mkwiyo wa mulungu udza pa ife, ndiponso adzatichotsa mu ufumu wake. (Aroma 1v18-32; 1 Akorinto 6 v 9-10)

Ngatitu nthawi ina yake tidachitapo zimenezi tidachitapo zimenezi , tisaganize kuti Mulungu sangatithandizenso kuti kudatha ai. Palitu chikhulupiriro kwa mulungu, choperekedwa kwa amene amvetsetsa chikhululukiro chakecho (Masalmo 130v4) Ekeleziya ya ku Akorinto idali ndi anthu ena amene adalapa: "Amenewo adali ena a inu; koma mwasambitsidwa (pobatizidwa) mu mdzina la Ambuye Yesu "1 Akorinto 6v9-11)

Tikaonetsetsatu mwa chilengedwe chathu mwamuna amasirira mkazi koma zoti munthu agonane ndi mwamuna mnzake zosenzi zikusonyeza kumulakwira , ndipo timakhala ndi mayesero opitirira ndithu. Mulungu sadzatileka ife kuyetsedwa kopitirira muzochitika zathu mpaka apeze njira yotichinjirza (1 Akorinto 10 v13) Pazochitika zonse za thupi, munthu akhoza kufika pena pozindikira kutimunthudi ayenera kukhala chonchi. Ndiyetu kuledzera kapena mankhwala osokoneza bongo ndi zinthu zmene ngati wazolowera sungathe kungokhala mpaka umweko basi ndipomunthu ayenera kusintha maganizo ake, ndipo atha kuthandizidwa ndi a zachipatala kuti abwere ku makhaliidwe abwino ngati kale.

Nawonso ogonana amuna okhaokha ayendenso mu ndondomeko yomweyi. Mulungu amuthandiza munthuyu nkuyesetsa kwake. Ngati munthu angadzipeleke kwathunthu pogonjetsa zofuna za thupi, Mulungu adzwawona anthuwa monga momwe adachitira ndi a Israeli akale:

Chifukwa chaichi Mulungu anawapeleka iwo kuzilakolako za manyazi: pakuti angakhale akazi ao anasandutsa machitidwe awo a chibadwidwe akhale machitidwe asalingana ndi a chibadwidwe cha a kazi, natenthetsana ndi cholakalaka chawo wina ndi mnzache, amuna okhaokha anachitirana chamanyazi, ndipo analandira mwa iwo okha mphoto yakuyenera kulakwa kwawo" (Aroma 1 v 26-27)

Apatu zikuonekeratu, munthu asakhale osawona ai, kutitu uneneriwi ukukhudzana kwambiri ndi matenda amene awanda masiku ano a EDZI, koma kuti ndi njira ina yoti matenda apatsirana kudzera mnjira yachiwerewere akufalikira.

11.5 KUSONKHANA MOGWIRIZANA

Mau oti kusunkhana mogwirizana ndimau amene akutithandiza kuzindikira kuti ndinjira yoti atha kulankhulana ndi kumvana bwino bwino. Pamene tikudziwa ndikuchita njira za mulungu, ndiye kuti tikugwirizana ndi iye ndinso ena amene achita chimodzimodzi pokhala mwa khristu.

Ndichapafupi kunyoza udindo umene tiri nawo pamene tisonkhana mogwirizana ndi anzathu: Kuchita chabwino ndi kusunkhana musayiwale "Ahebr 13v16). Afilipi 1v5 akukamba za kusunkhana mogwirizana kwathu mu uthenga wabwino" Pamene pagona mgwirizano wathu ndi chiphunzitso choonadi cha uthenga Wabwino. Pachifukwa chaichi kusunkhana mogwirizana kwa okhulupirira oonadi ndi kosiyana ndi magulu ena kapena mipingo ina. Pachifukwanso cha ichi amatha kuyenda maulendo atali kukakahalaq ndi anzawo, kuyendera abale amene ali kwaokha, komanso azigwiritsa ntchito

telefoni kapena makalata kuti alankhulane paliponse pamene izi zingatheke Paulo akuti "Kugwirizana mu Mzimu (Afilipi 2v1), zimene zikutanthauza apa ndi zakuti kukumana mogwirizana kwagona pa kutsata Mzimu/maganizo a mulungu mofanana monga mmene mau ake adalembedwera.

Chimodzi chapadera cha kukumana chogwirizana kwathu kwagona pakusunga chilangizo choti tizidya mgonero pamodzi. Okhulupirira akalewo adapitirira mu mchiphunzitso cha atumwi ndi kusunkhana mogwirizana (pakuchita) mgonero, mmapempherokudya mgonero....mokondwa ndi mtima umodzi (Machitidwe a Atumwi 2v42,46) Mgonerowu umaimiriratu chiyembekezo chathu chenicheni , ndinso pogawana zidzimanga ife pamodzi ndi mtima umodzi ""Chikho cha dalitso chimene tidalitsa, sichili chiyanjano cha mwazi wa khristu kodi? Mkate umene tinyema sulu chiyanjano cha thupila khristu kodi? Pakuti mkate ndiwo umodzi, chotero ife ambiri ndife thupilimodzi pakuti ife tonse titengako ku mkate umodzi kutanthauza kuti khristu (1 Akorinto 10v16-17) Nchoyenera kuti onse amene ntchito ya khristu ikuwapindulira agawane zoyamikira za nsembe ya khristu , amene ali akudya mkate umodzi| ndiokhawu amene adabatizidwa mwa khristu moonadi, atadziwadi choonadi, ndiwo ayenera kuchita ichi ndipo mchoyenera kugawana ichi ndi wina aliyense.

Yohane akutikumbutsa mmene adagawirana za moyo osatha ndi ena "kuti inunso mukhoza kusunkhana mogwirizana ndi kwa atate , ndi mwana wake Yesu khristu (1 Yohane 1v2,3)

Izi zikuonetsa kuti kusunkhana mogwirizana kwagona pakufanana zokhulupirira za mu uthenga wabwino, ndikubweretsa ife mu kusunkhana mogwirizana ndi anzathu okhulupirira, ndinso ndi mulungu komanso Yesu moonadi. Pamene tigwiritsa ntchito Uthenga wabwino mmoyo wathu, kugonjetsa zochimwa zathu zanthawi zonse, ndipo ngati tipitirira mu kumvetsetsa kwathu mau a mulungu, timazama mu kukumana kwathu mogwirizana ndi mulungu ndi khristu.

Kukumana mogwirizana kwathu ndi mulungu ndi khristu ndi okhulupirira ena sikuti kumangodalira kuzikhulupiriro zofanana zimene ziri zoonadi ai zimene ziri mu mchikhulupiriro chimodzi "koma moyo wathu uyenera ugwirizane ndi zimenezozo. Mulungu nkuunika ndipo mwa iye mulibe mdima ayi ngati tinena kuti tigwirizana ndi iye, ndipo tiyenda mdima, tikunama, ndipo sitikuchita

choonadi. Koma ngati tiyenda mkuwala monga iye ali kuwala, ndiye kuti tikukumana mogwirizana ndi anzathu, ndipo mwazi wa Yesu khristu mwana wake utitsuka ife tonse ku machimo onse" (1Yohane 1v5-7)

Kuyenda mu mdima kumatanthauza moyo umene utsutsana ndi kuwala kwa mau amulungu (Masalmo 119v105; Miyambo 4v18); Sizitanthauza machimo amene timachita mwakanthawi chifukwa zofooka zathu, vesi lina likuti, "ngati tinena kuti tilibe chimo, tidzinamiza tokha, ndi choonadi kutanthauza Mau a mulungu Yohane 17 v 17;3v21; Aefeso 5v13) Sichili mwa ife ai (Yohane 1 v 8)

Pamene tikumva zofunikirazi zikuthandiza kudziwa kuti kukumana mogwirizana kumatha ngati okhulupirira oyamba kutsatira ziphunzitso, kapena moyo wathu, zimene zimatsutsana ndi chiphunzitso cheni cheni cha baibulo "Musasonkhane mogwirizana ndi ochita ntchito za mudima, koma atsutseni iwo (Aefeso 5v11) Tiyetsetse kuti tiwabwezere potsata njira zabwino za m'busa wabwino amene afuna nkhoa yotaika (Luka 15v1-7)

Ngati m'bale apitirira kutsatira ziphunzitso zonama kapenanso makhalidwe osayenera, nkoyenera kuimika kukumana mogwirizana mwandondomeko yake (Mateyo 18 v15-17). Izi zimachitika poyendamo ndi m'baleyo kumufunsa kenaka kudziwitsa anthu onse awo ndi makhiradefiya polemba mbuku lawo limene amalandira nthawi zonse. Komabe, tisangoti ndondomeko igwire nchito nthawi yomweyo zachita koma kuti munthu amvetsetsedi kuti zimene Baibulo limaphunzitsa ndi izi ndipo kutinso pachifukwa wasokera nkoyenera kuimitsa kukumana mogwirizana ndi iye.

Palinso mau ena amene amatilangiza za kusunkhana mogwirizana pa 2 Akorinto 6V 14-18: Musakhale omangidwa mgoli ndi osakhulupirira osiyana; pakuti chilungamo chigawana bwanji ndi chosalungama.....Ndi chiphatikizo chake mchanji ndi kachisi wa mulungu ndi wa mafano?.....chifukwa chake Tulukani pakati pawo ndipo patukani.....Ndipo ndidzakhala kwa inu Atate, ndi inu mudzakhala kwa ine ana amuna ndi akazi, ananena Ambuye wamphamvu .

Tawonatu apa kuti kodi mau a mulungu ali kuunikadi mavesiwa akuti tisamasonkhana mogwirizana ndi mipingo ina imene imakhulupirira ziphunzitso zonama;Komanso chifukwa chimene tiskwatire/kukwatiwa ndi amene sadziwa

choonadi, ndikutinso tidzipatule ku njira za mdziko. Ngati tiphunzitsa monga kuyenera, ndichodziwikiratu kuti magulu amene amakhulupirira nkambakamwa ngati utatu kapena za mdiyerekezi kuti ndi chimngelo ayenera kutithawa chifukwa timaoneka kuti tikuwatsutsa.

Chiphunzitso ndi chofunika chifukwa chimatichinjiriza moyo wathu kuti tikhale monga mmene malembo aliri; choncho tiyenera kukhala angwiro mu chiphunzitso ngati tikuyesayesa kukhala moyo wa ngwiro. Makhalidwe athu amakhala kapena amayankha kapena kuvomereza zimene a mipingo ina amanena za satana ndi zitsanzo zina.

Pamene tidzipatula kunjira za mdziko. Ngati tiphunzitsa choonadi cha mulungu monga kuyenera, ndichodziwikiratu kuti magulu amene amakhulupirira nkambakamwa ngati utatu kapena za mdiyerekezi kuti ndi chimngelo ayenera kutithawa chifukwa timawoneka kuti tikuwatsutsa.

Chiphunzitso ndi chofunika chifukwa chimatichinjiriza moyo wathu kuti tikhale monga memene malembo aliri; choncho tiyenera kukhala "angwiro mu chiphunzitso" ngati tikuyesayesa kukhala

Moyo wa ngwiro. Makhalidwe athu amakhala kapena amayankha kapena kuvomereza uthenga wabwino umene tidaumva ndi kukhulupirira (Afilipi 1V27). Ziphunzitso zonse zonama zimaipitsa makhalidwe a Mulungu-pali zoti chilango chosatha 'hade', kapenanso kuvomereza zimene zimene a mipingo ina amanena za satana ndi zitsanzo zina.

Pamene tidzipatula kuzamdziko tiri ndi ulemerero wapadera odzakhala ana enieni a mulungu, kukhala ngati mbali imodzi ya banja limene liri lopezeka padziko lonse la abale ndi alongo. Palitu "thupi limodzi," kutanthauza kuti mpingo (Aefeso 1V23) limene liri ndi iwo akusunga chiyembekezo chimodzi-Mulungu mmodzi, ubatizo ndi chikhulupiriro chimodzi (aefeso 4V4-6). Nkovuta kukhala mbali imodzi ya thupi limodzili ndikumasonkhananso mogwirizana ndi ena a mipingo ina amene sakhulupirira choonadi. Pakutitu mdima sungasonkhane pamodzi ndi okhulupirira choonadi. Pakutitu mdima sungasonkhane pamodzi ndi okhulupirira choonadi tikatero ndiye kuti tasankha kusionkhana mogwirizana ndi mdima chimene sichifunika.

Ngati tithokozadi moonza ziphunzitso zoonadi zonse zimene zidaululidwa mmalembo, titha kuona kuti amene akhulupirira ziphunzitso zonama mu mdzina la chi Kristu sangasonkhane pamodzi ndi mulungu.

Ngati mwalondola bwinobwino zimene tawerengazi, tikhoza kuona kuti sikuti tingochita theka laziphunzitso timati tikakhala mu ubale ndi mulungu. Timakhalatu mwa Kristu mu ubatizo mwa iye, kapena kunja kwa iye. Tiritu mkuwala ngati tidziwa chiphunzitso choonadi ndi kuchimvera kapena apo ayi ngati sitimvera tikhala mundima ndi winanso.

Pamene tadziwa zinthu zapaderazi zimene ndi choonadi zimatipatsa udindo wapadera pamaso pa mulungu. Sitiyeneranso kapena kuwonetsa miyoyo yathu ngati munthu wa mdziko ai. Mulungu akutiwonetsa machitidwe athu pamodzi pake. Iyeyo, komanso Yesu Kristu ndi onse okhulupirira afunitsitsa kuti mudzichita zoyenera. Ndipo monga mulungu, Kristu ndi ifenso tiyesetsa kukuthandizani monganso mmene adachitira Mulungu popereka mwana wake ndikutifera ife-ndipotu mudziwitse kuti chipulumutso chanu chagona pa mmene inu mufunira, kapena titi mmene inu mwasankhira kuti musungedi chiyembekezo cha mtengo wapaderachi chimene chaperekedwa kwa inu.

PHUNZIRO 11: MAFUNSO

- (1) Kodi munthu amene afuna kuti abatizidwe ayenera kusintha motani mu moyo wake?
- (2) Kodi 'Kudziyeretsa kapena kudzipatula kutanthauzani?
 - (a) Kusalankhulitsana ndi osakhulupirira
 - (b) Kudzipatula ku za uchimo ndi kutumikira zinthu za mulungu
 - (c) Kupita ku chalichi
 - (d) Kuchitira zabwino anthu ena
- (3) Kodi ndi nchito ziti zimene okhulupirira oonadi sayenera kugwira?
- (4) Kodi mau oti oitanidwa(oyenera) ndi ekeleziya amanthauzani?
- (5) Kodi ziganizozo ziri mmusizi zowawa ndi ziti zofotokozera za mgonero?
 - (a) Tidzichita pafupi pafupi sabata iriyonse
 - (b) Tidzichita kamodzi pa chaka pa nthawi ya pasika
 - (c) Mkate ndi vinyo zimasintha kukhala thupi ndi mwazi weniweni wa Yesu.
 - (d) Mkate ndi vinyo zimaimiria thupi ndi mwazi wa Yesu.
- (6) Kodi ndi ziganizo ziti ziri zoonadi zofotokozera za ukwati?
 - (a) Tidzikwatira/kukwatiwa ndi okhulupirira enieni.
 - (b) Kuthetsa ukwati kuli kovomerezeka kwa okhulupirira
 - (c) Okhulupirira okwatiwa/okwatira amene mzakeyo ali osakhulupirira ayenera kukhala nawo.
 - (d) Pa banja mwamuna amyimirira Kristu ndi mkazi amayimirira okhulupirira.
- (7) Kodi azimayi ayenera kulalikira mu ekeleziya(mpingo)?
- (8) Kodi ngati mwabatizidwa mutadziwa choonadi, mudzapitirira kukumana mogwirizana ndi mipingo imene siphunzitsa choonadi?

(9) Kodi mufuna kuti mmodzi wa ma Khilisitafediya abwere kuti mudzakambirane zambiri za uthenga wabwino, ndipo potsiriza pake mubatizidwe?